Hakîkat Kitâbevi Publications No: 2

KIYI WA KHOMO LA KU JANNA

Bukhu Lofotokoza Njira yokalowera ku Janna (Mtendere)

Hüseyn Hilmi Işık

www.gofreebooks.com Hakîkat Publishing READ NOW

Hakîkat Kitâbevi Publications No: 2

KIYI WA KHOMO LA KU JANNA

Bukhu Lofotokoza Njira yokalowera ku Janna (Mtendere)

Lolembedwa ndi
Muhammad bin Qutb-ud-din Izniki

Lobwerezedwa ndi
Hüseyn Hilmi Işık

Hakîkat Kitâbevi
Darüşşefeka Cad. No: 53 P.K.: 35 **34083**
Fâtih-ÎSTANBUL
Tel: 0212 523 45 56-532 58 43 Fax: 0212 523 36 93
http://www.hakikatkitabevi.com.tr
e-mail: bilgi@hakikatkitabevi.com.tr
Januwale 2024

Zam`katimu

YALIYOMO.....Fehler! Textmarke nicht definiert.

Mau Oyamba Bukhu lofotokoza za njira yopita ku Jannah ..... **- 5 -**

BUKU LOFOKTOKOZA ZA NJIRA YOPITA KU JANNA ..... **- 8 -**

CHISILAMU ALLAHU TA'ÂLÂ ALIPO NDIPO NDI MMODZI..... **- 8 -**

ZIZINDIKIRO ZA IMAN ..... **- 18 -**

SIFAT-I-DHATIYYA ..... **- 19 -**

SIFAT-I-THUBUTIYYA..... **- 20 -**

ZAWJAT (AKAZI) NDI GHAZAWAT (MAULENDO) A MTUMIKI ..... **- 43 -**

TSATANETSATANE WA IMAN ..... **- 46 -**

ZOYAMBITSA KUSAKHULUPILIRA (KUFURU) ..... **- 50 -**

AHKAM AL-ISLAMIYYA..... **- 59 -**

NSICHI ZA CHISILAMU..... **- 65 -**

NAMAZ (SWALA) ..... **- 68 -**

GHUSL (KUSAMBA) ..... **- 70 -**

PEMPHERO LA TAWHID ..... **- 81 -**

HAID ndi NIFAS (Nsambo ndi Kutha kwa kubereka) ..... **- 82 -**

UDHU kapena KUZITSUKA..... **- 100 -**

ZA MADZI ..... **- 101 -**

KUGWIRITSA NTCHITO MISWAK (MSWACHI)..... **- 103 -**

MA MUSTAHAB A UDHU..... **- 104 -**

MAKRUH A UDHU..... **- 105 -**

ZOMWE ZIMAWONONGA UDHU ..... **- 105 -**

MAPEMPHERO ONENA POCHITA UDHU..... **- 107 -**

ZOKHUDZA TAYAMMUM..... **- 109 -**

ISTINJA, ISTIBRA, ndi ISTINQA..... **- 116 -**

KACHITA SWALAH..... **- 117 -**

ADHAN-I-MUHAMMADI ..... - 122 -

ADAB ZA SWALAH..... - 133 -

MAPEMPHERO (kapena Ma Dua woperekedwa) ..... - 135 -

ZOMWE ZILI MAKRUH PA SWALAH..... - 136 -

ZOWONONGA SWALAH ..... - 139 -

PHINDU LA SWALAH YA JAMA'AT ..... - 144 -

KUTSOGOLERA MU SWALAH YA JAMAAT (IMAMAT) ..... - 145 -

KUKHAZIKIKA PA SWALAH (TA'DIL-I-ARKAN) ..... - 146 -

SWALAH PA MAULENDO ATALI..... - 147 -

PHINDU LA TAKBIR YA IFTITAH ..... - 150 -

MINDA YA PAMWAMBA YA KU MPARADISO..... - 153 -

(JANNAT-I-ALIYYAT)..... - 153 -

MAPEMPHERO OSACHITIKA M'NTHAWI YAKE (Swalah za Qada) .. - 156 -

KUWOMBOLA WOMWALIRA KU NGONGOLE ZA SWALAH ..... - 164 -

SWALAH YA TSIKU LA CHISANU ..... - 169 -

KUYIMIKA SWALAH ..... - 178 -

KUKHALA NDI UDHR..... - 178 -

SWALAH NTHAWI YA MATENDA..... - 182 -

KUFUNIKIRA KWA SWALAH ..... - 185 -

KULIPIRA ZAKAT ..... - 197 -

KUSALA kapena KUFUNGA..... - 211 -

NSEMBE (QURBAN)..... - 221 -

HAJI (ULENDO WOPITA KU MZINDA WOPATULIKA WA MAKKA).. - 222 -

MA FARDH 54 ..... - 224 -

MACHIMO AKULU (GHUNAH-I-KEBAIR) ..... - 228 -

MALISECHE (AWRAT) ndi KUZIPHIMBA KWA AZIMAYI ..... - 234 -

ZOMUYENEREZA WOKHULUPILIRA ..... - 244 -

MAKHALIDWE OTAMANDIKA (AKHLAQ HAMIDA)..... - 246 -

ZOKHUDZA ULEMELERO WAKU CHIPEMBEDZO WA MA SAHABAH - 248 -

CHAKUDYA NDI MADIBWE ..... - 252 -

UKWATI..... - 256 -

KUSAMBISA, KUVEKA NDI KUYIKA MSILAMU WAKUFA ..... - 266 -

MITUNDU YA IMFA..... - 268 -

MFA YA ANA (OSACHIMWA)..... - 274 -

IMFA YA MZIMAYI WA CHISILAMU ..... - 276 -

IFA YA OFERA CHIKHULUPIRIRO ..... - 280 -

IMFA YA MUNTHU WOSAKHULUPIRIRA..... - 282 -

KUKAZONDA KU MANDA NDI KUWERENGA QU´RAN AL-KAREEM - 287 -

BUKHU LACHITATU KALATA YA CHISANU NDI CHINAYI (9) ..... - 291 -

BUKHU LA CHITATU, KALATA 84 ..... - 292 -

KALATA YA 114..... - 294 -

MFUNDO ZOTSIRIZA KUCHOKERA M'BUKU LA NJIRA YOPITA KU PARADISO..... - 298 -

KALATA YA 123..... - 302 -

KALATA YA ZANA NDI MAKUMI AWIRI NDI MBAMBU ZINAYI ..... - 303 -

Mau Oyamba
Bukhu lofotokoza za njira yopita ku Jannah (ku Mtendere)

Allahu ta'âlâ anatumiza Atumiki "alaihim-us-salâm" ake ndi ma umboni pamodzi ndi chiongoko kwa akapolo Ake ndi cholinga chowatulutsa mu mmdima wosochera ndi umbuli. Ndi kuwayika a kapolowo mu dangalira kuti apeze chisangalalo, chitonthozo ndi mtendere pa dziko pano ndi moyo wachiwiri pambuyo pa ifa. Pakutero akapolo a Allahu ta'âlâ ayenera kulumikizana mitima, wina ndi nzake, ngati abale ndi kuphunzira kugwira ntchito limodzi ngati akapolo Ake. Allahu ta'âlâ anakwaniritsa kudziwitsa akapolo Ake olengedwa, chikhalidwe chabwino kudzera mwa Atumiki Ake olemekezekawa. Allahu ta'âlâ analengeza kuti mwa Atumiki onse omwe anatumizidwa, Muhammad "alaihim-salâm" ndiye wa pa mwamba kuposa onse. Iye ndi Mtumiki wa anthu onse okhala pa dziko lino lapansi kuyambira pa nthawi yake mpaka kutha kwa dziko. Mu **Qur'an al-kareem, y**omwe Allahu ta'âlâ anayivumbulutsa kwa Mtumiki Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" pang'onopang'ono kwa zaka 23 kudzera mwa mngelo, muli Malamula ndi zoletsa zochokera kwa Allahu ta'âlâ. Chifukwa choti Qur'an al-kareem yomwe ikupereka maphunziro omveka ndi zizindikiro za nzeru inalembedwa mu Arabic, Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" anayifotokozera kwa omutsatira ake, ma Sahabah, "alaihim-ur-ridwân" kuchokera ku mayambiliro mpaka ku mapeto ndipo Iye anati: **"Aliyense yemwe angayifotokozere Qur'an al-kareem m'njira yosiyana ndi mafotokozedwe anga, adzakhala kafiri (osakhulupilira)".** Akatswiri a chipembedzo cha Chisilamu omwe anamva kuchokera kwa Ashab-i-kiram za mafotokozedwe a Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam", nawo analemba momveka bwino m'mabuku a **Tafsir** kuti aliyense amvetse. Akatswiri amenewa amatchedwa **Ahl as-Sunnat** (eni kutsatira za Mtumiki). Mabuku omwe analemba akatswiri a Ahl as-Sunnat anawalemba posankhaniza mafotokozedwe ochokera mu Qur'an al-kareem ndi mau a Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" omwe amatchedwa **hadith** ndipo zili m'mabuku a **Ilm-i-hal**. Aliyense wofuna kudziwa zoona ndi zokhazikika za Chisilamu zomwe Allahu ta'âlâ akuphunzitsa mu Qur'an al-kareem ayenera kuwerenga mabuku a **Ilm-i-hal**.

Chiyambi cha bukhu lino lomwe tathandauzira kuti **Bukhu lofotokoza za njira yopita ku Jannah** ndi **Miftah-ul-Janna**, kutanthauza kuti **Kiyi wa khomo la ku Janna**. Bukhuli linalembedwa ndi Muhammad bin Qutb-ud-din "rahima-hullâhu ta'âlâ" amene anamwalira ku Edirne m'chaka cha 885 Al Hijri (1480 AD).

Katswiri wina wozama pa chipembezo cha Chisilamu, Sayyid 'Abd-ul-Hakim Efendi "rahima-hullâhu ta'âlâ" (yemwe anabadwa mchaka cha 1281 [1865 A.D.] ku Bashkal'a, Van ndi kumwalira mchaka cha 1362 [1943 A.D.] ku Ankara ku Turkey) ananena kuti: "Mlembi wa bukhu lotchedwa **Miftah-ul-Janna** anali munthu woopa Allahu ta'âlâ. Chidzakhala chinthu chothandiza kwambiri kuŵerenga bukhuli." Pa chifukwa ichi tasindikiza bukhuli m'Chichewa kuti lithandize ambiri. Pakulongosola bukhuli muli ndemanga ndi mau ena m'mabulamketi omwe tabwereka kuchokera m'mabuku ena. Sindemanga zongofuna kukometsera kapena manganizo a munthu ayi. Tikupempha Allahu ta'âlâ kuti atiteteze tonse ku misampha ya adani a Chisilamu omwe akusintha ndi kupotoloza choonadi ponamizira kuti akugwira ntchito za Chisilamu, pogwiritsa ntchito mayina a Chisilamu komanso kudzera mwa anthu opembedza ndi odziwika m'chipembedzo. Allahu ta'âlâ atiteteze kuti tisanyengeke ndi kugawanika. Allahu ta'âlâ atilunzanitse ife tonse pogwiritsa ntchito potsatira Madhhab a **Ahl as-Sunnat**, yomwe ndi njira yokhayo yomwe tingaziyeretsere tokha potsatira Mtumiki Wake wokondedwa "sallallâhu alaihi wa sallam". Atidalitse ife tonse kuti tikhale okondana pakati pathu ndi othandizana wina ndi mnzake. Amin!

[Munthu asanachite chinthu chilichonse, limayamba ndi **ganizo** kapena **lingaliro** lomwe limadza mu mtima mwake kuti achite chinthucho. Cholingachi chimatchedwa kuti **niyya.** Munthu akapanga niyya, chotsatira ndi kulamula chiwalo kapena ziwalo zake kuti zichite chinthucho ndipo uku kumatchedwa **qasd** (kuyesera). Kugwira ntchito kwa ziwalozo kumatchedwa **kasb** (kuthekera)**.** Ntchito ya mtima imatchedwa **akhlaaq** (machitidwe, khalidwe). Maganizo kuti afike mu mtima, ali ndi magwero asanu ndi limodzi (6): **Wahy**, ili ndi Ganizo lochokera kwa Allahu ta'âlâ**.** Maganizo a wahy amadza mmitima ya Atumiki okha. Ganizo la **Ilhaam** (kudzoza) limabwera ndi Angelo ndipo limadza kwa Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" ndi mmitima ya **Asilamu a Salih** (Oyera, odzipereka komanso oopa Allahu ta'âlâ). Maganizo ochokera kwa Asilamu a salih amatchedwa **Nasiihat** (uphungu, malangizo). Maganizo ochokera kwa Satana mdyerekezi amatchedwa **waswasa** (kukayikitsa, kusocheretsa). Maganizo

achisanu amatchedwa **shahawah** ndipo gwero lake ndi nafs ya munthu[1] (chilakolako cha thupi/zokonda za thupi). Gwelo la maganizo otsiriza lomwe ndi lodzaza ndi gulu loipa limatchedwa **ighwa'u** (chinyengo). Wahy, ilhaam, ndi nasiihat ndi maganizo abwino ndi othandiza. Nasiihat kapena kuti uphungu, umaperekedwa kwa aliyense. Waswasa ndi shahawah zimabwera m'mitima ya anthu osakhulupilira ndi ma fasiq[2] Maganizo onse awiriwa ndi oipa komanso owononga. Zinthu zimene Allahu ta'âlâ amazikonda ndi kuzivomereza, zimatchedwa **halal** (zabwino), ndipo zimene sakonda zimatchedwa **ithm/haram** (zoipa, zauchimo). Allahu ta'âlâ, mwini chifundo chambiri, wafotokoza za halal ndi za haram mu **Qur'an al-kareem**. Allahu ta'âlâ watilamulira kuchita zinthu zabwino, ndipo watiletsa kuchita zinthu zoipa. Zinthu zomwe Allahu ta'âlâ walamula ndi zomwe waletsa pamodzi zimatchedwa **Ahkam Al-islamiyya** (Malamulo a Chisilamu). Mtima wa munthu womwe ungatsatire uphungu woperekedwa ndi ma **Salih** ndi kulingalira bwino komanso kudzisintha ndi kutsata Ahkam Al-islamiyya, udzakhala woyera ndi wodzaza ndi nûr (kuwala). Mtima umenewo udzapeza chisangalalo ndi mtendere pa dziko lapansi ndi tsiku lomaliza. Mtima wosamvera Ahkam Al-islamiyya koma kutsatira ma nafs ndi Satana pokhulupirira zosochera, zongomva ndi zowerenga zolembedwa ndi anthu oipa ndi zindiq, udzakhala wakuda ndi wovunda. Mtima woyera wodzadza ndi nûr udzasangalala pomvera Ahkam Al-islamiyya. Pomwe mtima womwe uli wakuda udzasangalala kutsatira magulu oyipa, ma nafs, ndi mdyerekezi. Allahu ta'âlâ, mwini wa chifundo amalenga mitima yoyera kwa ana onse obadwa pa dziko lapansi. Mitimayi imadzada ngati ya makolo awo potsata zochita za makolowo ndi zochita za magulu oyipa.]

[1] mphamvu yoipa yobadwa nayo m'thupi la munthu.

[2] Asilamu ochimwa, osamvera.

BUKU LOFOKTOKOZA ZA NJIRA YOPITA KU JANNA

Al hamdulillah alladhi ja'alanaa minattalibeena wa lil ilmi minarraaghbeena wassalaat wassalaamu alaa Muhammadin alladhi arsalahu Rahmatan lil Aalameena wa alaa aalihi wa As-haabihi Aj'maeen.

CHISILAMU
ALLAHU TA'ÂLÂ ALIPO NDIPO NDI MMODZI

[Allahu ta'âlâ alibe chiyambi ndipo alibe mapeto. Analipo, alipo ndipo adzakhalapo. IYE ndi amene analenga zolengedwa zonse. Sanapezeke pa mbuyo pa china chilichonse. Kukanakhala kuti IYE kunalibe pa chiyambi, ndiye kuti panayenera kukhala mphamvu yolenga IYE. Kuti chinthu chilengeke ndiye kuti pali mphamvu yolenga chinthucho. Popanda mphavu imeneyo chinthucho sichingalengeke chifukwa palibe wochilenga. Koma tikalankhula za Allahu ta'âlâ, palibe mphamvu inalipo yomwe inalenga IYE. Ngati tikutsutsa kuti mphamvu yolengayo inakhalapo pachiyambi, ndiye kuti payenera kukhala mphamvu ina yomwe inalenga mphamvu imeneyo. Izi zingatanthauze kuti pali chiwerengero chosawerengeka cha olenga. Popanda mlengi, ndiye kuti chilengedwe chonse cha kuthupi ndi cha uzimu chimene timaona kapena kumva bwenzi kulibe. Koma poti zinthu za ku thupi ndi moyo zilipo, ndiye kuti ziyenera kukhala ndi mlengi mmodzi yemwe ndi wamuyaya.

Allahu ta'âlâ anayamba ndi kulenga zinthu zoyambirira zomwe ndi tizigawo tomwe timapanga chinthu chirichonse cha thupi, mzimu ndi Angelo. Zinthu zoyambirira zimenezi ndi zomwe zimatchedwa elements (tizigawo). Pali tizigawo tokwana zana ndi mphambu zisanu (105)[1] tomwe zikudziwika lero. Allahu ta'âlâ analenga, ndipo nthawi zonse amalenga chinthu chirichonse kuchokera ku tizigawo 118 timeneti. Chirichonse mwa izi ndi gawo pa lokha monga, chitsulo (Iron), sulphur, carbon, mpweya wa okusijeni ndi mpweya wa chlorine. Allahu ta'âlâ sanafotokoze kuti ndi zaka ma miliyoni angati omwe adutsa chilengere zimenezi. Sanatiuzenso kuti anayamba liti kulenga dziko lapansi, kumwamba ndi za moyo pogwiritsa ntchito ma element amenewa. Cholengedwa chirichonse, chimakhala ndi nthawi yake

[1] Pomwe amalemba bukhuli pali tizigawo tokwana zana ndi mphambu zisanu (105) tomwe timadziwika, koma tsopano pali tizigawo tokwana zana ndi khumi ndi mphambu zisanu ndi zitatu (118) tomwe zikudziwika.

yokhalira kapena kupezeka chikapangidwa. Amalenga nthawi ikakwana ndi kuchiononga nthawi yake ikatha. IYE amalenga chinthu popanda pochokera komanso amatha kulenga china kuchokera ku chinthu china, pang'onopang'ono kapena mwadzidzidzi ndipo pomwe chatsopanocho chikupezeka, choyambacho chimatha.

Allahu ta'âlâ analenga munthu kuchokera ku mzimu ndi thupi lopangidwa ku zinthu zoti zilibe moyo. Kale lonse kunalibe Munthu. Allahu ta'âlâ analenga nyama, zomera, majini ndi Angelo asanalenge munthu woyamba. Munthu woyamba ndi bambo wathu Adam "alaihim-sallallâhu wa sallam". Ndipo kuchokera kwa Adam "alaihim-sallallâhu wa sallam", Allahu ta'âlâ analenga mkazi. Anthu onse padziko anachulukana kuchokera mwa awiriwa. Zinthu zonse, za moyo ndi zopanda moyo zimasintha. Koma chomwe chiri cha muyaya sichisintha. Zinthu zimasintha mmaonekedwe, mzochita, mzigawo komanso mmitundu nthawi ikamadutsa. Mankhwala akakhalitsa amatha mphamvu ngakhalenso mchikhalidwe chawo moti amakhonza kukhala poyisoni. Khungu limasuwa ndikuchoka chikopa pomwe chikopa china chimamererapo. Nyukiliya ikaphulika, tizigawo take timasintha ndi kusanduka mphamvu. Njira yopezekera chinthu china kuchokera ku chinthu china siyingakhale njira ya muyaya popanda chiyambi. Ziyenera kuti zinachokera ku zinthu zakale zomwe zinapangidwa posachokera pena paliponse. Pakuti umuyaya umatanthauzanso kupanda chiyambi.

Adani a Chisilamu omwe amanamizira kuti ndi a Science, amati anthu anachokera kwa anyani. Iwo amati izi zinanedwa ndi dokotala wa Chingerezi wotchedwa Darwin. Izi ndi zabodza. Dr. Charles Darwin (yemwe anabadwa mu 1809 ndi kumwalira mu 1882 A.D.) sananene choncho. Iye amafototokoza poyera za kulimbana kwa moyo pakati pa zolengedwa za moyo. M'buku lake lomwe mutu wake ndi woti: **The Origin of Species,** iye analemba kuti za moyo zinayamba kukhala ndi makhalidwe ogwirizana ndi malo amene zimakhala ndipo potero zinasintha pang'ono chabe. Sananene kuti za moyo zina zimasintha ndi kukhala zina zatsopano. Pa msonkhano wa bungwe la British Association for the Advancement of Science womwe unachitikira ku Salford mu 1980, Prof. John Durant wa pa yunivesite ya Swansea ananena kuti kulongosola kwa kusinthika komwe Darwin anena kokhuza chiyambi cha munthu kunasinthidwa kukhala nthano yamakono yomwe yawononga Science ndi kulepheretsa kupita pa tsogolo kwa chikhalidwe cha anthu. Nthano ya chisinthoyi "yakhudza kwambiri mu kafukufuku wa Science," zomwe zayambitsa "kupotoza

kwa zoona ndi mikangano yosafunikira, ndipo kwagwiritsidwa ntchito molakwikwa ku Science." Iye adatsimikiza kuti chiphunzitso cha Darwin tsopano chasiyana kwambiri, ndipo izi zadzetsa milu ya malingaliro owononga ndi osayenera.[1] Mawu a Prof. Durant onana za Darwin ndi ena mwa mayankho osangalatsa omwe amaperekedwa kwa okhulupirira a Darwin m'dzina la Science. Chifukwa chachikulu chomwe chimabwezeretsa mmbuyo kafukufuku masiku ano pa zokopa anthu pa mlingo wina wa chikhalidwe ndi chiphunzitso ichi cha chisintho chomwe ndi malingaliro chabe. Iwo alibe zolinga za Science. Chiphunzitso ichi chikugwiritsiridwa ntchito ngati chida chotengera nzeru za ku thupi. Mtsutso wakuti munthu anachokera ku anyani ndi maganizo chabe opanda gwero. Ndi bodza lamkunguniza lochokera kwa adani a Chisilamu wosadziwa Science. Sizomwe Darwin ananena ayi. Munthu wodziwa kapena wa Science sanganene mawu a umbuli ndi opusa ngati amenewa. Munthu amene wamaliza maphunziro a ku yunivesite, ndikukhala ndi moyo wotayilira, n'kuyiwala zimene waphunzira kusukulu, m'malo mopitiriza maphunziro ake a Science amene wachita bwino kwambiri, sangakhale munthu ozindikira kapena wa nzeru zakuya za Science. Choyipa kwambiri ndi kutengera udani wake ndi Chisilamu, ndikuyesa kufalitsa mawu ndi zolemba zake za bodza m'dzina la kuzindikira ndi Science. Potero amakhala ngati ka chilombo koyambitsa matenda komwe kamakhala kovulaza anthu. Zikatero digiri yake, ulemu wake ndi udindo wake zidzakhala misampha yokolera achinyamata. A Science aku Sham omwe amafalitsa ma bodza awo ndi miseche yawo m'dzina la kuzindikira ndi Science amatchedwa **a Science onyenga**.

Allahu ta'âlâ amafuna kuti anthu azikhala momasuka ndi mwa mtendere pa dziko la pansi koma kuti adzapeza chisangalalo chosatha pa tsiku lomaliza. IYE walamula zinthu zothandiza kudzetsa chisangalalo ndi kuletsa zinthu zowononga zomwe zingadzetse chiwonongeko. Munthu, kaya ndi wopembedza kapena ayi, wokhulupirira kapena ayi, ngati akutsata ndi kugwiritsa ntchito Ahkam Al-islamiyya, kaya mozindikira kapena mosazindikira, mlingo wa chitonthozo ndi mtendere umene adzaupeze m'moyo wa pa dziko lapansi udzakhala wolingana ndi khalidwe la kumvera kwake ku dongosolo la malamulowo. Fanizo la izi ndi munthu wodwala. Ngati akumwa mankhwala oyenera motsata ndondomeko yake, amachira ku matenda. Koma akamwa mankhwala olondola mosokoneza, mwina

[1] Dr. John Durant (pa University ya Swansea, ku Wales), kuyankhula momwe chisintho chinakhalira nthano ya Science "New Scientist," 11 September 1980, p. 765.

amachira movutikira kapenanso kufa ndi mankhwalawo. Anthu ambiri omwe sapembedza ndipo sakhulupirira, amapambana ndi kusangalala pa dziko pano chifukwa amapanga ntchito zawo m'njira yomwe ndi yovomerezedwa ndi Qur'an al-kareem. Koma sangasangalale kwa muyaya. Chisangalalo cha muyaya chidzapezeka pokhapokha ngati munthu akudziwa ndi kumvera Qur'an al-kareem.

Lamulo loyamba la Allahu ta'âlâ ndi kukhala ndi **iman**, ndipo **kufr** ndi chomwe IYE akuletsa pamwamba pa zoletsedwa zonse. Iman ndi kukhulupirira kuti Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" ndi Mtumiki womaliza wa Allahu ta'âlâ. Allahu ta'âlâ amampatsa Iye lamulo LAKE mu njira ya "Wahy". Anamuvumbulutsira Iye **Ahkam Al-islamiyya** kudzera mwa mngelo, ndipo Iye anafotokoza zonsezo kwa anthu. Qur'an al-kareem ndi mawu amene Allahu ta'âlâ anavumbulutsa kudzera mwa mngelo. **Mushaf** (kapena kuti **Msafu**) ndi bukhu lomwe lili ndi zolembedwa zonse za Qur'an al-kareem. Qur'an al-kareem si mawu ochokera kwa Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" koma ndi mawu a Allahu ta'âlâ. Ma ayah ake ndi a ngwiro ndipo palibe munthu amene angathe kunena kapena kulemba liwu ngakhale limodzi lofanana ndi ungwiro wa mau a mu Qur'an al-kareem. Malamulo onse omwe Qur'an al-kareem ikuphunzitsa pamodzi amatchedwa **Chisilamu**. **Mumin** (Okhulupirira) ndi munthu yemwe wakhulupirira malamulo onse a Chisilamu ndi mtima wake wonse ndipo iye ndi **Msilamu**. Kukanira kapena kusakonda ngakhale lamulo limodzi kumatchedwa **kufr (**kukanira malamulo ndi zomwe zaletsedwa ndi Allahu ta'âlâ). Kukhulupirira za kuti kudzakhala moyo pambuyo pa imfa; za kuti majini ndi Angelo alipo; za kuti Adam "alaihim-sallallâhu wa sallam" ndi kholo la anthu onse komanso ndi Mtumiki woyamba, ndi mfundo za chikhulupiliro cha mtima. Kukhulupirira kwa izi ndi chiphunzitso chokhudza **iman** kapena **itiqad** kapena **aqaid**. Zizolowezi zina ziyenera kutsatidwa ndipo zina zomwe ndi zoletsedwa ziyenera kupewadwa posazichita. Zizolowezi zonsezi ziyenera kukumbukiridwa mu mtima kaye zisanachitidwe kapena kupewedwa. Izi ndi ziphunzitso za **Ahkam Al-islamiyya.** Kukhulupirira Ahkam Al-islamiyya ndi gawo la iman. Kuchita kapena kupewa ndi **ibada** (kupembedza). Munthu akatsatira Ahkam Al-islamiyya atayamba kutsimikiza kaye mu mtima (kuchita niyya/cholinga), ndiye kuti wapembeza. Zomwe Allahu ta'âlâ walamaula ndi zomwe Iye waletsa zimatchedwa **Ahkam Al-islamiyya.** Zomwe Subhana Watala walamula kuti tizichita zimatchedwa **fardh** ndipo zomwe IYE waletsa zimatchedwa **haram.** Munthu wonyoza chimodzi mwa ntchito zimenezi ndi **kafir** (munthu wokanira choonadi akuchidziwa). Munthu

wonyalanyaza koma akukhulupirira si kafir. Iye amakhala Msilamu wa **fasiq** (munthu wophwanya malamulo). Mumin amene amakhulupilira ziphunzitso za Chisilamu ndi kuzitsatira molondoloza amatchedwa **Msilamu wa Saalih** (Msilamu wabwino). Msilamu yemwe amamvera chipunzitso cha Chisilamu ndi kukonda Murshid (aphunzitsi) ndi cholinga chopeza chisomo ndi chikondi cha Allahu ta'âlâ amatchedwa munthu wa **Saalih** (wabwino). Msilamu amene wapeza chisomo ndi chikondi cha Allahu ta'âlâ amatchedwa **Arif** kapena **Waliy** (mtetezi). Waliy yemwe amaphunzitsa anthu enanso kuti nawo apeze chikondi cha Subhana Watala amatchedwa **Murshid**. Anthu onse osankhidwawa, pamodzi, akutchedwa anthu a **Sadiq.** Onsewa ndi **Saaliheen**. Saaliheen sakalowa ku Jahena (ku moto). Ndithu, kafir adzakalowa ku Jahena ndipo sadzatuluka ku Jahena komwe adzapatsidwa mazunzo osatha. Kafir akakhala ndi iman ndi kukhala Msilamu, machimo ake onse amakhululukidwa nthawi yomweyo. Naye Fasiq akuchita tawba (kulapa) ndikuyamba kupembedza, sadzapita ku Jahena. Iye adzapita ku mparadiso mosazengereza chimodzimodzi ngati wokhulupirira wa Saalih. Koma pali njira ziwiri kwa Fasiq amene sachita tawba: kukhululukidwa ndi kukalowa ku Mparadiso atalandira **shafaah** (Pemphero la Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" lopempha Allahu ta'âlâ kuti amukhululukira) kapena popanda kulandira shafaah kuthandizidwa; kapena akaotchedwa ku Jahena moyenera ndi machimo ake ndipo kenako kukalowa ku mparadiso atamaliza chilango chake.

Monga tanena kale mmau oyamba, Qur'an al-Kareem inavumbulutsidwa m'chiyankhulo cha Chiarabu. Galamala yake inali yogwirizana ndi Chiarabu chomwe anthu amayankhula pa nthawiyo. Komanso Inalembedwa mwa ndakatulo. Choncho Qur'an al-Kareem ili ngati ndakatulo. Ndi yodziwika ndi kuya kwa chiyankhulo cha Chiarabu ndipo ndi yovuta kuyimvetsa. Ndiyovuta kuyimvetsetsa kwa munthu yemwe sanazame m'chiyankhulo cha Chiarabu, ngakhale ali odziwa kuwerenga Chiarabucho. Ngakhale anthu odziwa mwakuya chiyankhulochi, sanathe kuyimvetsa. Choncho Bwana wathu, Mtumiki wodalitsika "sallallâhu alaihi wa sallam", anafotokoza zambiri za iyo. Malongosoledwe a Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" a Qur'an al-kareem amatchedwa **hadith sharif** (zoyankhula za Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam"). As-hab-i-kiram (Masahaaba olemekezeka) "ridwânullâhi"[1] adapereka ziphunzitso zomwe anamva

[1] Chonde onani bukhu lotchedwa SAHABAH 'The Blessed' limodzi mwa zolembedwa za Hakikat Kitabevi.Fatih, Istanbul, Turkey.

kwa Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam” kwa mibado ya achinyamata yomwe inali nkudza pambuyo pawo. Ndi kudutsa kwa nthawi m’mitima mwa anthu munayamba kuchita mdima pang’onopang’ono. Asilamu olowa kumene atsopano anayesera kutanthauzira Qur’an al-Kareem ndi malingaliro awo ochepekedwa ndi osakhwima. Izi zinapereka matanthauzo osemphana ndi mafotokozedwe a Bwana wathu, Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam”. Ndipo adani a Chisilamu anayambitsa kugawanika ndi ming’alu mchikhulupiriro. Kunawoneka magulu makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri (72) omwe ndi achinyengo komanso a bodza. Asilamu omwe ali ndi zikhulupiliro zolakwika motere amatchedwa **anthu a bidah** (Obweretsa zachilendo m’chipembezo). Ndithu, magulu onse makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri a bidah adzalowa ku Jahena kukalangika. Koma pokhala kuti iwo ndi Asilamu, sadzakhala ku Jahena muyaya, adzatulutsidwa ku Jahena ndi kukalowa ku Mparadiso atamaliza chilango chawo.

Iman ya munthu imayamba kutayika pamene chikhulupiliro chake chisemphana ndi chimodzi mwa ziphunzitso zodziwika bwino; zomwe ndi ziphunzitso zafotokozedwa mu Qur’an al-kareem kapena m’hadith-i-sharif. Iye amatchedwa **mulhid** (Munthu yemwe watuluka Chisilamu). Mulhid amaganiza kuti iye ndi Msilamu**.**

Ahl as-Sunnat “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaihim” ajmaiin ndi akatswiri m’chipembezo omwe anaphunzira maphunziro a itiqad. Anaphunzira mfundo zolondola kuchokera kwa As-hab-i-kiram “ridwânullâhi” ndipo anazilemba ziphunzitsozo molondola m’mabuku. Iwo ndi akatswiri amene anafika pa mlingo wa ijtihad (kutha kumasulira malamulo pa okha) imodzi mwa Madhhab anayi. Akatswiriwa samatanthauzira Qur’an al-karim ndi malingaliro awo ayi koma ankakhulupirira zophunzira zochokera kwa As-hab-i-kiram “ridwânullâhi” . Amafalitsa njira yoona imene anaphunzira kwa Mtumiki wathu “sallallâhu alaihi wa sallam”, osati kutsatira nzeru zawo.

Munthu kuti ukhale wotetezedwa ku masautso a dziko la pansi ndi tsiku lomaliza, uyenera kukhala ndi iman monga akuphunzitsira akatswiri a Ahl as-Sunnat. Iman imapangitsa munthu kukhala ndi moyo wabwino ndi wa chimwemwe. Ndikofunika kuphunzira ndi kukhulupilira zochita zonse m’chisilamu. Anthu osakhulupilira chikhulupiriro cha Sunni amakhala **ahl-i-bid’at**, (Asilamu opatuka), kapena **mulhid (**yemwe ndi kafir, wosakhulupilira). Munthu wokhulupirira ayenera kuphunzira ndi kusunga mu mtima zenizeni za

Ahl as-Sunnat. Munthu ayenera kuphunzira Chisilamu pozindikira zoyenera kuchita ndi zoyenera kuzipewa ku thupi komanso mu mtima. Munthu uyenera kuchita ntchito zopembedza. Akatero azapeza chisomo ndi chikondi cha Allahu ta'âlâ. Akatswiri a Ahl as-Sunnat analongosola nkhani zopembedza m'njira zinayi zosiyana zomwe zimatchedwa **Madhhab** (njira zolondola za Chisilamu).[1] Mfundo zosiyana mnjira zinayizi, zimakhala zochepa komanso pa zinthu zazing'ono. Chifukwa choti mfundo zambiri zazikulu zimafanana, pali kuyanjana pakati pa Madhhabu anayiwa ndipo otsatira ake amakhala ochitirana chifundo ndi kulemekezana wina ndi mnzake. Msilamu aliyense ayenera kuchita mapemphero ake motsatira imodzi mwa Madhhab anayiwa. Munthu amene sangatsatire imodzi mwa Madhhab anayiwa adzakhala kuti wasiya Ahl as-Sunnat (njira yoona) ndi chowonadi. Izi zalembedwanso m'mutu wakuti "Dhebayih" wa Ahmad bin Muhammad bin Isma'il **Tahtawi's** "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (yemwe anamwalira mu 1231 [1815 AD] popanga ndemanga ya bukhu lotchedwa **Durr-ul-Mukhtar** lolembedwa ndi Alauddin Haskafi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (1021, Haskaf 1088 [1677 A.D.]).

Kafir (wosakhulupilira) akanena kuti: "Tsopano ndine Msilamu", ayenera kukhulupiliridwa, kaya ndi ogwidwa pa nkhondo kapena watero pa nthawi ya mtendere. Koma munthuyo adzayenera kuphunzira **nsichi zisanu ndi imodzi** za iman ndi kuzikhulupilira nthawi yomweyo. Kenako ayenera kuphunzira ndi kusunga malamulo a Chisilamu. Achite zomwe zakakamizidwa -fardh ndipo asiya zomwe zaletsedwa - haram. Aphunzire izi nthawi iliyonse komanso pamene wapeza danga. Kusaphunzira, kunyozera kapena kunyalanyaza chimodzi mwa zimenezi, ngakhale kuti waziphunzira, kudzakhala kunyalanyaza chipembedzo cha Allahu ta'âlâ. Ndipo kuti Iman idzakhala itatayika. Anthu amene amataya iman yawo motere amatchedwa **murtadd** (opatuka, ogalukira). Alipo ena mwa ma murtadd omwe amadzionetsera ngati anthu achipembedzo ndipo potero amasocheretsa Asilamu. Awa amatchedwa **zindiq.** Tisakhulupirire ma zindiq kapena mabodza awo. Monga zalembedwera patsamba zana limodzi ndi khumi ndi zisanu ndi chimodzi (116) la ndemanga ya bukhu la chi Turkey lotchedwa **Siyar-i-**

[1] Madhhab anayi okhudzana ndi machitidwe a Chisilamu omwe Chisilamu chikuloleza ndi: Hanafi, Shafi'i, Maliki, ndi Hanbali. Tsatanetsatane wa Madhhab anayiwa akupezeka m'mabuku a Hakikat Kitabevi ku Istanbul.

kabir,[1] komanso mu gawo lomaliza la mutu wonena za nikah (Kumangitsa ukwati kwa Chisilamu) ya osakhulupirira m'bukhu lotchedwa **Durr-ul-mukhtar** kuti; 'munthu amene wafika pa kutha msinkhu adzaweruzidwa kukhala murtadd (wopatuka, wogalukira) ngati sakuvomereza Chisilamu kapena kuganiza mmaganizo mwake kuti iye ndi Msilamu. Izi zizakhala choncho kaya iye akuchita izi chifukwa chosadziwa Chisilamu kapena chifukwa chotengeka ndi zofuna za dziko. Zalembedwanso mchigawo chomaliza cha mutu wofotokoza za nikah ya kafiri mu **Durrul-muhtar** kuti 'pamene mtsikana wa Chisilamu wapanga nikah atafika pakutha msinkhu koma asakudziwa Chisilamu, nikah yake imakhala yopanda pake.' Tingati amakhala murtadd. Adzayenera kuphunzira zizindikiro za Allahu ta'âlâ. Adzayenera kubwereza zomwe akumva ndi kunena kuti, "Ndimakhulupilira". Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ" akufotokoza nkhaniyi motere: "Pomwe mtsikana ali wamng'ono (wosatha msinkhu) iye ndi Msilamu, chifukwa chipembedzo chake chiyenera kukhala cha makolo ake." Akadzatha msinkhu sadzadaliranso makolo ake pa chipembedzo. Akafika pakutha msinkhu ali mbuli ya chipembedzo cha Chisilamu, amakhala murtadd. Munthu yemwe wamva ndi kudziwa ziphunzitso za Chisilamu koma osakhulupilira si Msilamu; ngakhale atanena Kalima-i-tawhid: "**La ilaha il-l-Allah Muhammadun Rasulullah,"**. Msilamu ndi munthu yemwe amakhulupirira nsichi zisanu ndi imodzi zomwe ndi: "Amentu billahi..." ndipo nanena kuti: "Ine ndikuvomereza malamulo, omwe ndi zofunika kuchita ndi zomwe waletsa Allahu ta'âlâ,". Ndi chinthu choumilizidwa kwa Msilamu aliyense kuona kuti ana ake aloweza nsichi zisanu ndi imodzi za chikhulupiliro cha Chisilamu) zomwe ndi mawu akuti: "Aamantu billah wa Malaykatihi wa Kutubihi wa Rusulihi wal Yawmil aakhir wabil Qadari khayrihi wa sharrihi min- Allahu ta'âlâ wal ba'athu ba'adal mawt haqqun. Ash-hadu an laa ilaaha illallahu wa ash-hadu anna Muhammadan Abduhu wa rasooluhu."ndipo awaphunzitse bwino zomwe zikutanthauza. Mwana amakhala murtadd akafika pa msinkhu ngati: sakhulupilira nsichi zisanu ndi imodzi zimenezi;

[1] Bukhu limenelo linalembedwa ndi Muhammad bin Hasan bin Abdullah bin Tawus bin Hurmuz Sheybani (Imam Muhammad) "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (135 [752 AD], Wasit - 189 [805 AD], Rey), mmodzi mwa akatswiri a Chisilamu ophunzitsidwa ndi Imam Abu Hanifa "rahmatullâhi 'alaih". Shems-ul-aimma Abu Bakr Muhammad bin Ahmed "rahmatullâhi 'alaih"(d. 483 [1090 AD]) adalemba ndemanga m'bukuli, ndipo ndemangayo idaperekedwa mu Chituruki ndi Khwaja Muhammad Munib Efendi waku 'Ayntab (d. 1238). AH).

sakhulupilira imodzi kapena ena mwa malamulo ndi zoletsedwa za Chisilamu ndipo sakunena kuti amazikhulupirira izi. [Tsatanetsatane wa nsichi zisanu ndi imodzizi zikupezeka m'bukhu lotchedwa **Chikhulupiriro ndi Chisilamu,** limodzi mwa mabuku osindikizidwa ndi Hakikat Kitabevi ku Istanbul).] Msilamu aliyense, ana olowa m'malo mwa msilamuyo komanso omwe amadziwana nawo awerenge bukhuli. Pakutero adzalimbikitsa Iman yawo. Tisamale kwambiri kuti ana athu asaleredwe ngati ma murtad kuyambira ali ang'ono. Tiwaphunzitse iman, Chisilamu, udhu, ghusl (kusamba), ndi namaz (Swala!) Ntchito yaikulu ya makolo ndi kulera ana awo ngati Asilamu.

Zalebedwa motere m'bukhu la **Durer wa Ghurer**[1]**:** "Mwamuna amene wakhala murtadd ayenera kuuzidwa kuti akhale Msilamu. Kukayikira kwake kuyenera kulongosoledwa bwino ndi kuchotsedwa. Ngati atapempha nthawi yoti alingalire kaye, adzakhala mu ndende masiku atatu. Ngati achita tawba (kulapa chifukwa cha tchimo lake lalikulu ndi kupempha chikhululuko kwa Allahu ta'âlâ, polonjeza kuti sadzachita tchimo lalikululo), tawba yake idzalandiridwa. Akapanda kuchita tawba ndiye kuti adzaphedwa ndi (Msilamu) woweruza. Mkazi amene wakhala murtadd sadzaphedwa. Adzamangidwa ndi kusungidwa mndende mpaka atakhala Msilamu. Akathawira ku darul-harb (dziko lomwe si la chisilamu), sakhala Jariya nthawi yonse yomwe iye adzakhale ku darul-harb. Akagwidwa adzakhala Jariya. Akakhala murtadd nikah yake idzakhala yachabechabe. Sadzakhala ndi udindo pa chuma chake chonse, (sichidzakhalanso chuma chake). Chidzakhalanso chuma chake ngati atakhalanso Msilamu. Akamwalira kapena kuthawira ku dziko lomwe si lachisilamu, kapena kukhala murtadd ali ku darul-harbko, chuma chake chidzakhala cha amlowa mmalo wake. Ngati alibe mlowa mmalo, chumacho chidzalandiridwa ndi anthu omwe ali ndi magawo ovomerezeka kuchokera ku Bayt al-mal (nyumba ya chuma) Murtad sangalandire chuma kuchokera kwa murtad wina.

Katundu kapena chuma chopangidwa ndi murtad pomwe iye (mwamuna kapena mkazi) ali murtad sichidzakhala chake. Chidzakhala **fay** kwa Asilamu. Zochita zake zonse zachitukuko monga kugula ndi kugulitsa, mapangano obwereketsa, ndi kupereka mphatso, zidzakhala **batil** (zosaloledwa). Koma ngati atakhalanso Msilamu, zonse zidzabwerera monga kale ndikukhala sahih ndipo sikudzafunika kuchita qadha pa mapemphero omwe anamudutsa. Koma Haji yokha

[1] Yolembedwa ndi Muhammad Molla Husraw "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", wachitatu Ottoman Shaikh-ul-islam

adzayenera kuchitanso. Ntchito za chipembezo zitatu zoyambilira zomwe wokhulupilira watsopano ayenera kuphunzira ndi ghusl (kusamba), udhu (kudziyeretsa) ndi kuchita Namaz (swala).

Nsichi zisanu ndi ndi imodzi (6) za Iman ndi izi: Kukhulupirira kuti Allahu ta'âlâ alipo ndipo ndi M'modzi, ndi (kukhulupirira) chikhalidwe chake; kukhala ndi Iman (kukhulupirira) mwa Angelo; kukhulupirira mwa Atumiki; kukhulupirira m'mabuku akumwamba omwe anavumbulutsidwa; kukhulupirira kuti pali moyo pambuyo pa imfa; kukhulupirira kuti zabwino ndi zoyipa zonse zimachokera kwa Allahu ta'âlâ (Qada ndi Qadar). Nsichi iliyonse idzafotokozedwa payokha.

Tiyenera kusunga malamulo a Chisilamu ndi kupewa zoletsedwa zonse mu mtima komanso ku thupi. Mitima yathu ikhale tcheru kuopera kuti ingalowe mu ghafla (kusokonezedwa pa nkhani ya Allahu ta'âlâ) kudzera mu kuyiwala, kusazindikira kapena kufowoka. Ndikovuta kwambiri kuti thupi la munthu likhazikike mu Chisilamu ngati: mtima wake siuli tcheru, sakumbukira za kukhalapo ndi ukulu wa Allahu ta'âlâ ndi kukoma kwa madalitso a ku mParadiso ndi kuoopsya kwa moto wa Jahannam.

Ophunzira ozama a Science ya Chisilamu yotchedwa **Fiqh** yomwe imaphunzitsa malamulo a Chisilamu ndi zoletsedwa amatulutsa ma fatwa. Awa ndi mayankho operekedwa ndi ovomerezeka m'Chisilamu pa mafunso Asilamu okhudza njira zochitira mapemphero awo.)[1] Zimachokera kwa anthu awa otumikira Allahu ta'âlâ kuonetsetsa kuti zisakhale zovuta kuzichita. Kuti thupi livomereze Chisilamu mwachangu, momasuka komanso modzipereka, ndikofunika kuti mtima ukhale woyera. Munthu yemwe akudziwa kufunika kwa kuyera mtima ndi kukhala ndi khalidwe la bwino koma ndi kulekelera thupi lake osachita za Chisilamu, ndiye kuti iyeyo ndi **mulhid** (wachinyengo). Anthu amenewa amachita zozizwitsa zambiri monga kudziwitsa anthu zobisika (kulosela), kuchiza anthu ofowoka powapumira kapena njira zina. Izi zimatchedwa **istidraj** ndipo zidzawakokera ku Jahena ochitawo ndi owachemelera omwe. Chizindikiro cha mtima umene uli woyera ndi nafs imene ili mutmainna (yokhazikika) ndi thupi lomwe likudzisintha modzipereka ku Chisilamu. Kuyankhula koti, "Mtima wanga ndi woyera. Onani mu mtima mwanga," komwe amayankhula anthu koma popanda kusintha muzochita molingana ndi Chisilamu, ndi mawu opanda pake. Amangozinyenga okha ndi anthu omwe ali pafupi nawo.]

[1] Gwero la fatwa liyenera kuwonetsedwa kumapeto kwa fatwa.

ZIZINDIKIRO ZA IMAN

Akatswiri a maphunziro a Ahl as-Sunnah amanena kuti iman ili ndi magawo asanu ndi limodzi:

AMANTU BILLAHI: Kukhulupirira mwa Allahu adhîm-ush-shân. Allahu ta'âlâ alipo ndipo ndi M'modzi.

IYE alibe sharik kapena nadhir. (Alibe mnzake kapena wofanana naye. Sadalira wina kapena china chirichonse).

IYE ndi munazzah ku makan (mfulu pa malo). (Alibe malo enieni wopezekapo koma ali pena paliponse).

IYE ndi muttasif kamal (ali ndi ndi zizindikiro Zake za ungwiro). Ali ndi zizindikiro zodzadza bwino.

IYE ndi wangwiro ndipo alibe chizindikiro chopanda ungwiro. Zopanda pache mwa Iye mulibe. Ndithudi zizindikiro za ungwiro ziri mwa Iye. Ife ndi amene tili ndi zizindikiro zopanda ungwiro.

Zizindikiro zosowa ungwiro zomwe tili nazo ndi kupereŵera, monga: kukhala opanda manja kapena mapazi kapena maso, matenda ndi thanzi, kudya ndi kumwa, ndi zina zambiri zomwe zisali zokwanira mwa ife.

Zizindikiro zomwe Allahu ta'âlâ ali nazo ndi zizindikiro za kukwanira monga: kulenga Kwake kwa dziko lapansi ndi kumwamba ndi zolengedwa zonse zosiyanasiyana zomwe zimakhala mu mlengalenga, m'madzi, padziko lapansi ndi pansi pa nthaka; Kusunga zolengedwa Zake zambiri nthawi zonse, zina mwa izo timazidziwa koma zina zambiri zomwe sitingathe kuzimvetsetsa chifukwa cha kuchepekedwa kwa nzeru za umunthu wathu; kupereka Kwake rizq (chakudya ndi zina zosunga moyo) kwa zolengedwa zonsezi. Izi ndi zizindikiro Zake zina za ungwiro. Iye ndi qadir-i-mutlaq (Wamphamvu zonse). Cholengedwa chilichonse ndi ntchito yochokera ku zizindikiro za Kamal za Allahu ta'âlâ.

Pali zizindikiro makumi awiri ndi mphambu ziwiri (22) zomwe zili za Allahu ta'âlâ ndipo zili wajib (zofunikira) kwa ife kuzidziwa. Ndiponso IYE ali ndi zizindikiro zina makumi awiri ndi mphambu ziwiri (22) zomwe zili muhal (sizoyenera kumuganizira IYE ndipo ndi zosatheka kukhala nazo IYE.)

Zizindikiro zimenezi ziri mwa Allahu ta'âlâ. Mwa IYE mulibe zizindikiro za muhal. Muhal ndi mawu otsutsana ndi wajib. Zikutanthauza kuti: "sizingakhale".

Pali chizindikiro chimodzi chomwe chimatchedwa sifat-i-nafsiyya ya Allahu ta'âlâ ndipo ndi wajib kwa ife kuti tidziwe: **Wujūd,** kutanthauza "kukhalapo".

Umboni wotsimikizira pa chikhalidwe kuti Allahu ta'âlâ alipo ndi qawl-i-sharif Yake (mawu Ake a mdalitso) oti: **"Innani Anaallahu,"** (Nditudi ine ndi Allah). Umboni wotsimikizira m'maganizo kuti palidi Mlengi ndi zolengedwa zomwe tikuziwonazi. Payenera kuti pali yemwe analenga zolengedwa zonsezi. Ndi kosatheka kuti Iye asakhalepo.

Sifat-i-nafsiyya imatanthauza kuti Dhat (munthu) wopanda IYE ndipo IYEwopanda Dhat sangabadwe kapena kuganiziridwa.

SIFAT-I-DHATIYYA

Pali zizindikiro zisanu zokhudza Allahu ta'âlâ zotchedwa Sifat-i-dhatiyya ndipo ndi wajib kuti tizidziwe: Zimadziwikanso kuti **Zizindikiro za Uluhiyyah**, (umodzi wakuoembedza).

1- **Qidam** kutanthauza kuti palibe chiyambi cha kukhalapo kwa Allahu adhîm-ush-shân.

2- **Baqa** kutanthauza kuti palibe mapeto a kukhalapo kwa Allahu adhîm-ush-shân, zomwe zimatchedwanso wajib-ul-wujud. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima yachitatu yomwe Allahu ta'âlâ analengeza mu Surah Hadid. Umboni wamaganizo ndi woti, ngati kukhalapo Kwake kunali ndi chiyambi ndi mathero, Akanakhala wosakhoza ndi wopanda ungwiro. Ndipo wosakhoza ndi wopanda ungwiro sangathe kulenga chirichonse. Ketero ndi muhal (zosatheka) kuti Akhale ndi chiyambi kapena mathero.

3- **Qiyamhu bi-nafsihi,** kutanthauza kuti Allahu adhîm-ush-shân ndi odziyimira pa Yekha. Sasowa thandizo la a liyense mu Dhat Yake, mu zizindikiro Zake, kapena muzochita Zake. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima yomaliza ya Surah ya Muhammad "alaihim-salâm". Umboni wamaganizo ndi woti akanakhala kuti Alibe zizindikiro zimenezi akanakhala wosakhoza ndi wopanda ungwiro. Kukhala wosakhoza kapena kusakwanira ndi muhal kwa Allahu ta'âlâ.

4- **Mukhalafat al-hawadith,** kutanthauza kuti Allahu ta'âlâ ndi wosiyana ndi aliyense, mu Dhat Yake komanso mu zizindikiro Zake. Palibe chomwe tingafanizire Allahu ta'âlâ. Umboni wake mwa mwambo ndi zomwe Allahu ta'âlâ ananena mu ayah ya khumi ndi imodzi ya Surah Shura. Poganizira, umboni ndi wakuti, Akanakhala kuti Iye ndi wofanana ndi china chake, ndiye kuti akanakhala wosakhoza

ndi wopanda ungwiro. Kukhala wosakhoza kapena kusakwanira ndi muhal kwa Allahu ta'âlâ.

5- **Wahdaniyyat** kutanthauza kuti Allahu ta'âlâ alibe sharik (ophatikana naye) kapena nadhir (wofanana naye), kuyambira mu Dhat Yake, mu zizindikiro Zake ngakhale mu zochita Zake. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima yoyamba ya Allahu ta'âlâ mu Surah Ikhlas. Poganizira umboniwa izi ndi kuti Iye akanakhala ndi ophatikana naye zolengedwa zonse bwenzi kulibe; poti pamene wina akufuna kulenga china chake, mnzakeyo naye bwenzi akufuna kulenga china.

[Malinga ndi akatswiri ambiri a Chisilamu, **Wujūd** yomwe ikutanthauza kukhalapo, ndi chizindikiro cha padera. Motero pali zizindikiro zisanu ndi chimodzi pansi pa mutu wa **Sifat-i-Dhatiyya.]**

SIFAT-I-THUBUTIYYA

Mu Sifat-i-thubutiyya muli zizindikiro zisanu ndi zitatu (8) za Allahu Allahu adhîm-ush-shân zomwe ziri wajib kwa ife kuti tidziziwe. Zizindikirozi nazi: Hayat, Ilm, Sam, Basar, Irada, Qudrat, Kalam ndi Takwin.

Manthauzo a zizindikiro zimenezi ali motere:

1– **Hayat -** Allahu ta'âlâ ndi wa moyo. Umboni wake mwa mwambo ndi gawo loyambilira la ayah mu Surah Baqara ndime 255. Pa maganizo umboni ndi woti Allahu ta'âlâ akanakhala wopanda moyo zolengedwa izi sizikanakhalapo.

2- **Ilm** - Allahu ta'âlâ ndi mwini kuzindikira. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima ya Allahu ta'âlâ mu Surah Hashr ndime ya 22. Polingalira umboni ndi wakuti Allahu ta'âlâ akanakhala kuti ndi wosazindikira ndiye kuti akanakhala wosakhoza ndi wopanda ungwiro. Kukhala wosakhoza kapena kusakwanira ndi muhal (zosatheka) kwa Allahu ta'âlâ.

3- **Sem -** Allahu ta'âlâ ndi wakumva. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima yoyamba ya Allahu ta'âlâ mu Surah Isra. Polingalira umboni ndi woti, Iye akanakhala wopanda mphamvu ndi wopanda ungwiro kukanakhala kuti ndi wosamva. Ndi muhal kuti Allahu adhîm-ush-shân akhale wosakhoza kapena wopanda ungwiro.

4- **Basar** - Allahu ta'âlâ amaona. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima ndime yoyamba ya Allahu ta'âlâ mu Surah Isra. Polingalira umboni ndi woti Allahu ta'âlâ akanakhala wosapenya ndiye kuti akanakhala wopanda mphamvu komanso wopanda ungwiro

chifukwa chosowa kupenya. Kukhala wosakhoza kapena kusakwanira ndi muhal kwa Allahu ta'âlâ.

5- **Irada -** Allahu ta'âlâ ndi wofuna. Chilichonse chimene wafuna chimachitika. Palibe chingachitike pokhapokha atafuna. Anafuna (kuti kukhale) zolengedwa ndipo anazilenga. Umboni wake mwa mwambo ndi Surah Ibrahim mu ayah ya Allahu ta'âlâ ndime ya 27. Polingalira umboni ndi woti Iye akanakhala wosafuna ndiye kuti akanakhala wosakhoza komanso wopanda ungwiro. Ndipo kulephera kapena kusakwanira ndi muhal (chosatheka, mosemphana ndi chowonadi, kuchoka pamalopo) zokhudza Allahu ta'âlâ.

6- **Qudrat** - Allahu ta'âlâ ndi wa mphamvu zonse. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima ya Allahu ta'âlâ Surah Al-i-Imran ndime zana limodzi ndi makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zisanu (165). Polingalira umboni ndi woti Iye akanakhala wopanda mphamvu ndi wopanda ungwiro akadakhala kuti alibe mphamvu zonse. Ndipo ndi muhal kwa Allahu ta'âlâ kukhala wosakhoza kapena wopanda ungwiro.

7- Kalam - Allahu ta'âlâ ali ndi zoyankhula. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima ya Allahu ta'âlâ mu Surah Nisa ndime zana limodzi ndi makumi asanu ndi limodzi mphambu zinayi (164). Polingalira umboni ndi woti Iye akanakhala wopanda zoyankhula ndiye kuti bwenzi ali wosowa kuyankhulako kotero akanakhala woperewera. Ndipo kukhala woperewera ndi kusakhala wangwiro ndipo ndi muhal kwa Allahu ta'âlâ.

8- **Takwin** - Allahu ta'âlâ ndi wolenga, mwachitsanzo, Iye ali ndi mphamvu zolenga, kotero kuti amalenga. Iye yekha ndiye amalenga zonse popanda kanthu. Palibe mlengi wina pambali pa Iye. Umboni wake mwa mwambo ndi ayat-i-karima ya Allahu ta'âlâ mu Surah Zumar ndime ya 62. Polingalira umboni ndi woti Iye ali ndi zolengedwa zosiyanasiyana pa dziko la pansi ndi kumwamba, ndipo Iye ana lenga zonsezi Yekha. Kungakhale kufr, (kutaya iman), kunena kuti, "Mlengi," kwa wina aliyense kusiya Iye. Munthu sangalenge chilichonse.

Allahu adhîm-ush-shân ali ndi ma Sifat-i-manawiyya asanu ndi atatu (zosakhala za kuthupi) omwe ndi wajib kuti tizidziwe: Hayyun, Alimun, Sami'un, Basirun, Muridun, Qadirun, Mutakallimun,[1] Mukuwwinun.

Tanthauzo la zizindikiro zodalitsikazi ziri motere:

[1] Matembenuzidwe ena mu zilembo za Chilatini adapangidwa kuti athandize owerenga kupeza matchulidwe olondola momwe angathere a mawu aumisiri.

1- **Hayyun**: Allahu ta'âlâ ndi Wamoyo.

2- **Samiun**: Allahu ta'âlâ ndi wakumva. Uku ndi kumva kosagontha mpaka muyaya (sami qadim).

3- **Basirun:** Allahu ta'âlâ ndi wopenya. Iye amaona china chirichonse nthawi iriyonse mpaka muyaya.

4- **Muridun:** Allahu ta'âlâ ndi wofuna komanso irada-i-qadimi (chifuniro chake ndi chamuyaya).

5- **Alimun**: Allahu ta'âlâ ndi wozindikira. Iye amazindikira chirichinse ndipo ndi ilm-i-qadimi (kudziwi mpaka muyaya)

6- Qadirun: Allahu ta'âlâ ndi wamphamvu komanso qudrat-i-qadima (mphamvu zake nzosatha).

7- Mutakallim: Allahu adhîm-ush-shân ndi mwini kuyankhula ndipo ndi kalam-i-qadim (zoyankhula Zake ndi zamuyaya).

8- Mukewwinun: Allahu ta'âlâ ndi wolenga, ndipo amalenga chirichonse.

Zizindikiro za kusakhala kwa Allahu adhîm-ush-shân ndi zosagwirizana ndi zomwe tazitchulazi.

WA MALAIKATIHI: Ndikukhulupilira mwa Angelo Allahu adhîm-ush-shân; Ndili ndi iman mwa iwo. Allahu adhîm-ush-shân ali ndi Angelo. Adawalenga kuchokera ku nur (kuwala, Kuunika). Iwo ndi ma jism (alibe matupi). Sadya kapena kumwa. Si amuna kapena akazi. Amatsika ku dziko lapansi kuchokera kumwamba ndi kukweranso kupita ku mwamba. Amawoneka m'maonekedwe osiyanasiyana. Amamvera Allahu adhîm-ush-shân nthawi iliyonse. Samachimwa ngakhale kwaka nthawi kochepa ngati nthawi yomwe imatenga diso kuti liphetire. Mwa iwo muli muqarrab (oyandikana ndi Allah) ndi Atumiki.

WA KUTUBIHI: Ndikukhulupiliranso m'mabuku (akumwamba) a Allahu adhîm-ush-shân. Allahu adhîm-ush-shân ali ndi Mabuku. Pali mabuku okwana zana ndi anayi (104) omwe atchulidwa m'Qur'ân al-kerîm. Zana mwaiwo ndi mabuku ang'onoang'ono. Iwo amatchedwa **"Suhuf"**. Suhuf ndi mchuluko wa sahifa, ndipo sahifa ikutanthauza kuti 'tsamba' kapena 'thabuleti'). Ndiye pali mabuku anayi akuluakulu. **Torah** lomwe linavumbulutsidwa kwa Hadrat Mussa (Mose) "alaihim-salâm", **Zabur** lomwe linavumbulutsidwa kwa Dawud (David) "alaihim-salâm", **Injil** lomwe linavumbulutsidwa kwa Issa (Yesu) "alaihim-salâm", ndi **Qur'an al-karim** yomwe inavumbulutsidwa kwa Mtumiki wathu Muhammad "alaihim-salâm". Bukhu lotchedwa **"Could not Answer",** likufotokoza mwatsatanetsatane zambiri zokhudza mabuku

a **Torah** ndi **Baibulo** omwe ndi mabuku omwe akuŵerengedwa ndi Ayuda ndi Akristu amakono.

Pa mabukhu (100) ang'onoang'onowa, khumi (10) anatumizidwa kwa Adam "alaihim-salâm".Makumi asanu (50) anavumbulutsidwa kwa Seth "alaihim-salâm", makumi atatu (30) anatumizidwa kwa Idrissa "alaihim-salâm", ndipo khumi (10) kwa Ibrahima "alaihim-salâm". Onsewo anavumbulutsidwa ndi Jebrail "alaihim-salâm". Qur'an-i-'adhîm-ush-shân ndi bukhu lomaliza mwa mabuku onse ovumbulutsidwa kuchokera ku mwamba. Kutsika kwa Qur'an al-kerîm kudatenga zaka makumi awiri ndi mphambu zitatu (23). Imatsika pang'onopang'ono komanso m'ma ayat, ndipo malamulo ake adzakhalapo mpaka mapeto a dziko. Ndi yotetezedwa kuchiwonongeko ndi kusinthidwa kapena kuyipitsidwa ndi anthu. Ilibe zinthu zopanda pake, ngakhale kuchokera ku zowonjezera za anthu,

WA RASULIHI: Ndilinso ndi iman mwa Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât".

Allahu ta'âlâ ali ndi Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât". Atumiki onse ndi anthu. Adam "alaihim-salâm" ndi Mtumiki woyamba, ndipo Mtumiki wathu Muhammad Mustafa "alaihim-salâm" ndi Mtumiki womaliza. Atumiki ena ambiri "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" anadza napita pakati pa awiriwa. Allahu ta'âlâ ndi Yemwe amadziwa chiwerengero chawo.

Pali zizindikiro zisanu zomwe ziri wajib kwa ife kuti tidziwe za Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât": Sidq, Amanat, Tabligh, Ismat ndi Fatanat.

Sidq (Kukhulupirika): Atumiki onse "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" ndi okhulupirika m'mawu awo. Chilichonse ananena ndi chowona.

2- **Amanat** (kusunga): Samaswa phangano lomwe analonjeza.

3- **Tabligh** (kudziwa ndi kudziwitsa): Amadziwa malamulo onse ndi zoletsedwa zonse za Allahu ta'âlâ ndipo amazifalitsa kwa Ummat awo.

4**- Ismat** (ungwiro): Atumiki "alaihim-salâm"ali kutali ndi khalidwe lochita za uchimo. Sachita machimo akulu ngakhale ang'ono. Atumiki "alaihim-salâm"ndi gulu lokhalo la anthu opanda tchimo. Ma Shiia amati palinso gulu lina la anthu lopanda tchimo.

5– **Fatanat:** Kutanthauza kuti Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" onse ali ndi nzeru kuposa anthu ena.

Pali zizindikiro zisanu zomwe ndi jaiz (zololedwa, zotheka) kuti Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" akhale nazo: Amadya ndi

kumwa; amadwala; amamwalira, (ndi anthu oti amafa); amasamuka kuchokera dziko lina (pa dziko lapansi) kupita dziko lina (lomwe ndi tsiku lomaliza); Sakonda za mdziko.

Pali Atumiki makumi awiri ndi mphambu zisanu ndi atatu (28) omwe maina awo odalitsika alembedwa mu Qur'an-i-'adhîm-ush-shân. Malinga ndi akatswiri a chipembedzo, ndi wajib kwa aliyense kuwadziwa Atumikiwa.

Mayina a Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" ndi awa: Adam, Idrissa, Nuh, Shis, Hud, Swaleh, Lut, Ibrahim, Ismail, Ishaq, Yaqub, Yusuf, Shaibu, Ayyub, Zulkifl, Mussa, Harun, Dawud, Sulayman, Ilyas, Elyasa, Yunus, Zakariyya, Yahya, Isa, and Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam". Pali kusagwirizana za mayina a Uzayr, Luqman, ndi Zulqarneyn. Akatswiri ozama pa maphunziro a Chisilamu ena akuti anthu atatuwa komanso Khidr "alaihim-salâm" anali Atumiki. Pomwe akatswiri ena akuti anali ma Awliya (okhala pafupi ndi Allahu ta'âlâ). Zalembedwa mu kalata ya makumi atatu ndi mphambu zisanu ndi chimodzi (36) m'gawo lachiwiri la bukhu la Maktubat-i-Ma'thumiyya[1] kuti pali zonenedwa zotsimikizika za chikhalire za akatswiri zoti Khidr "alaihim-salâm" anali Mtumiki. Monga zafotokozedwe m'kalata ya 182 kuti kuoneka kwa al-Khidr "alaihim-salâm" ndi kuchita kwake kwa zinthu ngati munthu sikukuonetsa kuti iye ali moyo. Allahu ta'âlâ walola kuti mzimu wake ndi mizimu ya Atumiki ambiri ndi Awliya iwoneke m'mawonekedwe a thupi la umunthu. Kuwawona sikumasonyeza kuti ali ndi moyo.

Komanso ndikofunika kwa inu kunena kuti: Alhamd-u-lillah, Ine ndine mbadwa ya Hadrat Adam "alaihim-salâm" ndipo ine ndi m'modzi mwa Ummat (okhulupirira, Asilamu) wa Mtumiki wotsiriza Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam". Ma Wahhabi amatsutsa zoti Adamu " "alaihim-salâm" anali Mtumiki. Pachifukwa ichi, iwo amati Asilamu amaphatikiza Allahu ta'âlâ ndi zina. Iwo ndi makafiri (okanira).

WAL YAWMIL AKHIRA: Ndiponso, ine ndikukhulupirira kuti kuli tsiku lachiweruzo. Poti, Allahu ta'âlâ watidziwitsa za izi. Tsiku la Qiyama likuyambika pamene anthu adzauke m'manda. Lidzapitilira mpaka anthu atafika kumalo kwawo (omwe ndi) ku Mparadiso kapena ku moto. Tonsefe tidzafa ndipo pambuyo pake tidzakhalanso ndi moyo. Ndikukhulupirira kuti kuli Mparadiso ndi Jahannama; mizan

[1] Yolembedwa ndi Muhammad Ma'thum Faruqi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (1007, Serhend – 1079 [1668 A.D.], malo omwewo), mwana wachitatu wa Hadrat Imam Rabbani "quddisa sirruhuma".

(masikelo) ndi mlatho wa Sirat (mlato wowolokera phompho la ku Jahannama ndi kulumikiza dziko la pansi ndi paradiso, pomwe olungama okha ndi omwe adzathe kuwoloka ndipo osalungama adzagwere ku chilango cha moto); nashr (kuuuka kwa akufa) ndi hashr (kusonkhanitsidwa ku bwalo la chiweruzo); zoti ndi zoona kuti kuli kuzunzidwa m'manda ndi kufunsidwa mafunso ndi angelo awiri otchedwa Munkar ndi Nakir. Ndikukhulupirira kuti zonsezi ndithu zidzachitika.

WA BIL-QADARI KHAYRIHI WA SHARRIHI MINALLAHI TA'ÂLÂ

Ndikukhulupiliranso kuti zomwe zinachitika ndi zomwe zidzachitike, zabwino kapena zoipa zinachitika ndi zomwe zidzachitike ndi chikhonzero (taqdir) cha Allahu adhîm-ush-shân. Zonse zimachitika motsatira kudziwa Kwake ndi lamulo Lake. Ndipo amalenga mu nthawi yomwe anakhazikitsa ndi kuzilemba mu **Lawh al Mahfuz.**[1] Ine ndiri ndi iman imeneyo. Mu mtima mwanga mulibe chikayiko konse.

Ashhadu an la ilaha illallah wa ash hadu anna Muhammadan abduhu wa rasuluh.

Madhhab anga mu ziphunzitso za chikhulupiliro (i'tiqad) ndi Madhhab a **Ahlus Sunnah wal jamaah**. Ndimakhulupilira Madhhab amenewa. Mfundo zomwe magulu ena makumi asanu ndi awiri mphambu ziwiri (72) amavomereza ndi zolakwika komanso za chinyengo. Adzapita ku Jahannama.

[Asilamu omwe amakonda Ashab-i-kiram (maswahaba) "alaihim-ur-ridwân" amatchedwa kuti ndi a gulu la **Ahl as-Sunnah**. Ashab-i-kiram onse anali ophunzira ndipo ndi Asilamu a chilungamo (adil). Iwo anakhala pa ubwenzi (sohbat) wodalitsika ndi bwana wa anthu onse, Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam", ndipo amathandizana naye. Swahaba yemwe anali pa ubwenzi wochepera ndi Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ndi wapamwamba kuposa Wali yemwe ali wapamwamba pa Awliya (ambiri) yemwe si Swahaba. Khalidwe la maganizo auzimu analipeza iwo pokhala pa ubwenzi ndi wokondedwa wa Âkomanso ungwiro womwe adaupeza chifukwa cha mawonekedwe odalitsika ndi mapumidwe Ake, sizingaonekere kwa wina aliyense yemwe sanakumane ndi Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam".

Ashab-i-kiram "radiyallâhu ta'âlâ alaihim ajma'in" anali otetezedwa ku zilakolako za ma naf awo atangopanga ubwenzi ndi

[1] Lawh al Mahfuz ndi manthu wa mabukhu, momwe mwalembedwa zonse zomwe zinachitika ndi zomwe zidzachitike.

Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam“. Ife talamulidwa kukonda ma Ashab-i-kiram “radiyallâhu ta’âlâ alaihim ajma'in”. Zalembedwa motere m’masamba oyamba a ndemanga ya bukhu lotchedwa **Shir’at-ul-islam**:[1] “Yankhulani mwaulemu momwe mungathere za Ashab-i-kiram “alaihim-ur-ridwân”. Osayankhula zoipa za aliyense wa iwo.” Koma kwa magulu 72 opotoka aja: ena anawonjezera za nkhaniyi, pomwe ena anali osokera m’menemo; ena mwa iwo anakhulupirira za m’maganizo awo, pomwe ena anasochera ndi nzeru za chi Giriki. Kotero ankachita zinthu zomwe zinali zosemphana ndi Chisilamu. Iwo anakakamira za bidah, (zikhulupiliro ndi machitidwe omwe si a Chisilamu omwe anayambitsidwa mu dzina la zikhulupiliro ndi machitidwe a Chisilamu-zongowonjezera). Iwo anasiya Sunnah, yomwe ndi maziko a Chisilamu. Panaoneka anthu omwe anali ndi mkwiyo ndi anthu otchuka a Chisilamu, monga Abu Bakr as-Siddiq ndi Hadrat Umar “radiyallâhu ’anhumâ”, Omwe ndi opambana mwa Ashab-i-kiram malinga ndi kugwirizana kwa akatswiri pa maphunziro a Chisilamu (ijma). Koma mkwiyo umene ena mwa iwo amaumva sikukanalepheretsa kumveka kwa dzina lodalitsika la Bwana wathu, Mtumiki “alaihim-salâm”. Panali anthu ena omwe anatsutsa zoti Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam”, anatengedwa kupita kumwamba mu thupi ndi mu uzimu pa usiku wotchedwa Miraj.

Ndi zodabwitsa kuona omwe amazitcha ophunziro a Chisilamu a kuyankhula mmalo mwa gulu lotchedwa **Isma’iliyya**, lomwe ndi lowononga kwambiri mwa magulu 72 a bidat. Iwo akuyesetsa kusokoneza ndi kuwononga mibado ya achinyamata yosalakwa polemba ndi kufalitsa mabodza osiyanasiyana owononga. Amayipitsa mbiri ya makolo odalitsika a Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam” kuti anali osakhulupirira. Amafalitsanso zoti Mtumiki “alaihim-salâm” anali kupha nyama zoperekedwa nsembe pa maso pa mafano asanakhale Mtumiki. Palinso mabuku ena achi Shiite olimbikitsa kupotoloza anthu ndikutanthauzira kwawo kolakwika. Ndi zachiziwikire kuti zolinga za ogonja oterewa ndi kunyozetsa chipembedzo cha Chisilamu, kuba iman ya achinyamata ndi kuwasocheretsa. Âyat-i-kerima mu Qur’an ikunena kuti: **“Munthu amene amasulira Qur’an al-kerim molingana ndi maganizo ake adzakhala wosakhulupirira.”**

Akatswiri a Chisilamu anali ndi **adab** (Makhalidwe abwino monga momwe Chisilamu chimaphunzitsira). Iwo amaganiza mozama

[1] Yolembedwa ndi Muhammad bin Abu Bakr “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih” (d. 573 [1178 A.D.]). Ndemanga yake inalembedwa ndi Ya’qub bin Sayyid ‘Ali “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih” (d. 931 [1525 A.D.]).

asanayankhule kapena kulemba kuti asalakwitse. Amayankhula mosabwelera m'mbuyo. Mwachitsanzo, kunena zolakwika ndi kupewa kunena za m'maganizo awo mu dzina la Chisilamu. Koma kupeza mfundo zowona kuchokera mu **Edilla-i-shar'iyya**, omwe ndi magwero anayi akuluakulu a chiphunzitsa cha Chisilamu. Izi sizinthu zomwe Msilamu wamba angachite ndipo sichapafupinso kwa akatswiri a Chisilamu. Tichenjere ndikupewa zowononga chikhulupiliro. Tipewe mawu odetsedwa ndi zolemba za anthu omwe ndi mbuli zosazindikira ukulu wa Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" kapena Ashab-i-kiram "ridwânullâhi ta'âlâ 'alaihim ajmain" zomwe zili ngati utsi wakupha.

Mawu a Persion mu Chichewa:

Ndimanjenjemera ngati tsamba la msondodzi ngati ataukira iman yanga.

Allahu ta'âlâ awonjezere chikondi cha okondedwa Ake m'mitima mwathu. Atiteteze kuti tisagwere mng'anjo ya moto wokonda adani Ake! Chizindikiro chakukhala ndi iman mu mtima ndi kukonda wokondeka a Allahu ta'âlâ ndi kuwada adani Ake.

Pali Madhhab (sukulu za maligaliro) anayi mu **amal** (machitidwe a Chisilamu - zopembedza, ntchito ndi zochita zake): Awa ndi Madhhab a Imam Abu Hanifa, Imam Shafi'i, Imam Malik, ndi Imam Ahmad bun Hanbali "rahmatullâhi 'alaihim".

Ndikofunika kusankha ndi kutsata imodzi mwa Madhhab anayiwa. Madhhab onse anayi ndi owona ndipo ndi olondola. Onse anayi ali m'gulu la Ahl as-Sunnah. Tili mu Madhhab a Imam azam (Imam wamkulu). Asilamu otsatira Madhhab amenewa amatchedwa ma Hanafi. Tinene motere: "Madhhab a Imam a'zam ndi thawab[1] ndipo ndi olondola. Komanso ndi zotheka kuti si olondola. Madhhab ena atatuwo ndi wolakwika. Komanso ndi zotheka kuti atha kukhala olondola".

Zinthu zisanu ndi chimodzi (6) izi zizithandiza iman kukhala mwa munthu mpaka muyaya popanda kuchoka.

1- Ife tinakhala ndi Iman mu ghaib (zosaonekera). Iman yathu ili mu zobisika, zomwe sizinadziwike, osati mu zahir (zodziwika, zowoneka). Popeza kuti sitingathe kumuona Allahu ta'âlâ ndi maso athu. Komabe takhulupirira, takhala ndi iman ngati kuti tanamuwona. Sitinakhalepo ndi chikayiko chirichonse ponena za izi.

[1] Liwu loti "thawab" limagwiritsidwa ntchito ponse paŵiri mlongosoli ndi nauni. Khalidwe lina likakhala la thawab, ndiye kuti Allahu ta'âlâ akulikonda kwambiri ndipo pa tsiku lomaliza adzapereka malipiro.

2- Padziko lapansi ndi kumwamba, mwa anthu, majini, angelo, ndi Atumiki “alaihim-us-salawâtu wattaslimât” palibe cholengedwa ndi chimodzi chomwe chimadziwa za Ghaib. Allahu adhîm-ush-shân yekha, ndi amene akudziwa za ghaib, ndipo amapereka chilichonse chimene wafuna cha ghaib kwa zolengedwa zimene wazisankha. [“Ghaib” ndi chinachake chimene sichingazindikirike ndi ziwalo kapena kumveka mwa kuwerengetsera kapena kuyeselera. Ghaib imadziwika kwa okhawo amene awapatsa kudziwa ghaib.]

3- Kuzidziwa za haram kuti ndi za haram ndi kuzikhulupilira choncho.

4- Kuzidziwa za halal kuti ndi za halal ndi kuzikhulupirira choncho.

5- Kusadzimva kukhala wotetezedwa ku chilango cha Allahu adhîm-ush-shân, ndi kumuopa nthawi zonse.

6- Kusataya chiyembekezo cha chifundo cha Allahu adhîm-ush-shân ngakhale utakhala wochimwa chotani.

Ngati munthu sakwaniritsa chimodzi mwa zinthu zisanu ndi chimodzi izi ngakhale atakwaniritsa zisanu mwa izo, kapena ngati wakwaniritsa chimodzi mwa izo ndipo osakwaniritsa zisanu mwa izo, Imani ndi Chisilamu cha munthuyo sizidzakhala Sahih.

Pali zinthu makumi anayi [40] zomwe zingachititse munthu yemwe ali ndi iman pa nthawiyo kutaya iman:

1– Kugwiritsa bidah. Kukhala ndi chilema mu iman yake. Kupatuka pang’ono pa ziphunzitso zophunzitsidwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunnah kudzamuchititsa wopatukayo kukhala wampatuko kapena wosakhulupilira. Ngati munthu akana chinthu chokakamizidwa kuchikhulupilira, munthuyo amakhala kafir (wosakhulupilira) nthawi yomweyo. Ndi bidah kukana chinthu chomwe chili chokakamizidwa kuchikhulupilira. Bidah ikhoza kuchititsa munthu kufa opanda iman.

2– Iman yomwe ili yofooka. Iman yopanda yopanda ntchito zokakamizadwa kapena kupembedza (amals).

3- Kulolela kuti ziwalo zako zisanu ndi zinayi zisiye kutsata njira yoyenera.

4- Kupitiriza kuchita machimo akulu. Asilamu sayenera kumwa mowa, ndipo amayi ndi atsikana a Chisilamu asamawonetse mitu yawo, tsitsi lawo, akatumba, ndi manja awo kwa amuna omwe Sali mahram[1] kwa iwo.

5- Kusiya kuyamika chifukwa chodzimva kudalitsika ndi Chisilamu.

6- Kusalabadira zoti ungadzapezeke opanda iman pa tsiku lomaliza.

7- Kuchita nkhanza.

8- Kusamvera adhan-i-Muhammadi yomwe ikuchitika motsatira mmene Sunnah yalamulira. Munthu wosalabadira adhan ikuchitika amakhala kafiri kotheratu.

9- Kusamvera makolo. Kukana malamulo awo omwe ali ogwirizana ndi chiphunzitso cha Chisilamu omwe ali mubah (ololedwa) mwaukali.

10- Kulumbira pafupipafupi ngakhale zili zoona.

11- Pochita namaz, kunyalanyaza posalongosola machitidwe a izi: Ruku (kuweramitsa thupi mosayenera), Qawma (kuimilira pa mbuyo pa ruku), Sajda ziwiri (kugwada ndi kugwesa nkhope pansi pa Namaz), ndi Jalsa (kukhala chowongoka pakati pa ma sajida awiri). Pochita Namaz munthu uyenera kukhazikika ndikunena mau onse ofunika pa sitepe iliyonse.

12- Kukhala ndi maganizo oti Namaz ndi chinthu chosafunika, kusaona kufunika kophunzira namaz ndi kuphunzitsa banja lako ndi ana ako komanso kulepheretsa ena kuchita namaz.

13- Kumwa hamr (vinyo) ndi chakumwa china chilichonse choledzeretsa chikamwedwa kwambiri; lamulo limeneli limagwira ntchito ngakhale mowawo wamwedwa ochepa.

14- Kulowetsa okhulupilira m'mavuto.

15- Kunama kuti ndinu Wali kapena kudzionetsera kuti ndinu ophunzira mu Chisilamu. Kudzionetseranso ngati munthu wopembedza, mlaliki, popanda kuphunzira ziphunzitso za Ahl as-Sunnah. [Musawerenge mabuku achipembedzo olembedwa ndi onyenga komaso abodza otere. Ulaliki ndi zokamba zawo zisagwiritsidwe ntchito.]

16- Kuyiwala utchimo wako; ndikuzitenga mopepuka.

17- Kudzikuza ndi kudzimva kupambana kwambiri.

18- Ujb (kudzitamandira), kudzitamandira kuphunzira ndi kupembedza.

19- Kukhala munafiq, ukapirikoni, kukhala ntemakuwiri.

20- Njiru, kuchitira nsanje m'bale wako Msilamu ngakhaleso ena.

21- Osamvera malamulo a boma kapena bwana wako (ngakhale) malamulowo sakutsutsana ndi Chisilamu. Kuwukira malamulo awo otsutsana ndi Chisilamu.

22- Kunena kuti uje ndi munthu wabwino popanda kumuyesa.

23- Kukhala wabodza wachikhalire.

24- Kuwapewa ophunzira mozama za Chisilamu. [Kusawerenga mabuku olembedwa ndi a ophunzira a Ahl as-Sunnah.]

25- Kulekelera masharubu kukula motalika kuposa malire omwe anakhazikitsidwa ndi Sunnah.

26- Kwa amuna kuvala chovala cha siliki. Ndi zololedwa kuvala siliki wopangidwa kapena zinthu zopangidwa ndi siliki wolukidwa ndi thonje.

27- Kukhala ndi chizolowezi chojeda.

28- Kubweretsa mavuto kwa oyandikana nawo, ngakhale atakhala osakhulupirira.

29- Kusonyeza mkwiyo wochuluka pa zinthu za dziko.

30- Kulandira ndi kupereka chiwongola dzanja.

31- Kuvala mwamatama zovala zazitali manja kapena masiketi atali kwambiri.

32- Kuchita za ufiti ndi matsenga.

33- Kunyalanyaza kukamuchezera m'bale wako (mahram) amene ndi Msilamu owopa ndi omvera.

34- Kunyansidwa ndi munthu wokondedwa ndi Allahu ta'âlâ ndi kukonda anthu omwe (mukudziwa kuti) ndi oyipitsa Chisilamu.

35- Kumusungira mangawa m'bale wako Msilamu kwa nthawi yoposa masiku atatu.

36- Kukhala ndi chizolowezi chochita dama (chiwerewere).

37- Kuchita mathanyula ndi kusachita tawba[1] pambuyo pake. (Mathanyula ndi kulowetsa dheker kumbuyo kwa munthu wina. Dheker [chida cha mwamuna] ndi chiwalo chimene mwamuna amagwiritsa ntchito pokodza. Chiwalo cha mkazi chomwe chimagwiritsidwa ntchito pa yomweyi chimatchedwa ferj [ndata]).

38- Kuchita adhan (kapena azan) mu nthawi zosiyana ndi momwe zalembedwera m'mabuku a Fiqh kapena kuti mosatsatira zomwe

[1] Kuchita tawba pa tchimo linalake kapena machimo a munthu ndiko kulapa chifukwa cha tchimolo kapena iye, kupempha chikhululuko kwa Allahu ta'âlâ, ndi kumulonjeza kuti sadzachimwanso kapena iwowo.

Sunnah imanena; kapena kusasonyeza ulemu woyenelera atamva Adhan ikuchitika m'njira yovomerezeka ndi Sunnah.

39- Kuona munthu akuchita munkar (haram), iwe ndi kumulekelera osachita nahy (osamuletsa munthuyo) pomuyankhula mwaubwino, ngakhale kuti ungathe kutero.

40- Kulekelera akazi omwe mungawalangiza kuchita zoletsedwa m'Chisilamu. Awa ndi monga akazi anu ndi ana anu akazi omwe mwachitsanzo amatuluka mmakhomo osaphimba bwino ndi moyenelera mitu yawo, mikono, ndi miyendo, kapena kuziphoda ndi kuzitsira ma pelefumu onunkhira.

Iman ndi kulengeza kwa lilime ndi kutsimikizira mu mtima pa mfundo zomwe Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" adapereka kuchokera kwa Allahu ta'âlâ. **Chisilamu** chikutanthauza kukhala ndi Iman mwa Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" ndikuchita ntchito (amal) za chiphunzitso chake.

Komanso, **Din** ndi **Millat** ndi zofanana. **Din** kapena **Millat** zimatanthauza i'tiqad, kutanthauza mfundo zovomerezeka, zomwe Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" adabweretsa kuchokera kwa Allah adhîm-ush-shân.

Chisilamu kapena **Ahkam Al-islamiyya** zimatanthauza amal zomwe ndi mfundo zothandiza, zomwe Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" anabweretsa kuchokera ku Haqq taala.

Ndipo, iman-i-ijmali (chikhulupiliro modula), komwe ndi kukhulupilira mwachidule kudzakhala kokwanira kuti munthu akhale Msilamu. Sikofunikira kufotokoza mozama kapena kudziwa iman mozama. Muqallid iman, chomwe ndi chikhulupiliro cha munthu popanda kuzindikira, chidzakhala sahih, (chokwanira, chomveka.) komabe kudzakhala kofunikira kuzindikira mozama pa zinthu zina.

Pali milingo itatu ya iman: Iman-i-taqlidi, iman-i-istidlali, ndi iman-i-haqiqi.

Iman-i-taqlidi (chikhulupiriro chotsanzira). Munthu yemwe ali pa mlingo uwu wa iman sadziwa fardh, wajib, Sunnah, kapena mustahab. Amatsanzira makolo awo pa zimene amakhulupilira ndiponso polambira. Iman ya anthu oterowo ndi yosadalilika.

Iman-i-istidlali (chikhulupiriro chochokera m'maumboni a m'mabuku). Munthu yemwe ali pa mulingo uwu wa iman amadziwa fardh, wajib, mustahab ndi haram, ndipo amamvera Chisilamu. Iye ndi wozindikira komanso amazitsata za chikhulupiriro. Aphunzira

kuchokera kwa ophunzitsa za chipembedzo ndi mabuku. Iman ya anthu otero ndi yolimba.

Iman-i-haqiqi (chikhulupiliro choona, chenicheni). Ngati zolengedwa zonse zitasonkhana pamodzi ndi kugwirizana zomukanira Mbuye wawo (Allahu ta'âlâ), munthu wa mlingo uwu wa Iman sangamukane (Allahu ta'âlâ). Sangakhale ndi kachikayiko kalikonse ngakhale kochepe mumtima mwawo. Iman yawo ndi yofanana ndi ya Anbiy (Atumiki). Mulingo uwu wa iman ndi wa pamwamba koposa milingo iwiri inayo.

Malamulo a Chisilamu amakhudza amal (zochita, ntchito zopembedza), osati iman (chikhulupiriro, njira za chikhulupiliro). Iman, yokha, ndiyokwanira kulowa mu Mparadaiso. Pomwe ndizosatheka kukalowa ku m'mparadiso ndi ntchito zopembedza zokha popanda Iman. Iman yopanda amal ndi yovomerezeka, koma Amal yopanda iman ndi yopanda ntchito. Anthu opembedza, ochita zabwino, ndi kupereka sadaka koma opanda Iman, ntchito zao sizidzawachitira ubwino tsiku Lomaliza. Iman siyingaperekedwe ngati mphatso kwa munthu wina, pamene thawab yopezedwa mwa njira ya amal ikhoza kuperekedwa ngati mphatso. Munthu sangapereke kapena kulemba malangizo okhudza Iman mu chifuniro chake chomaliza. Koma akhoza kulangiza olowa m'malo mwake kuti adzamuchitire amal (iye akadzafa). Munthu wonyalanyaza amal sakhala wosakhulupilira. Koma amene wasiya Iman kapena kupeputsa Amal adzakhala kafiri. Munthu amene ali ndi chifukwa chokwanira (udhr) kapena amene sangathe adzaloledwa kusiya amal. Koma palibe munthu amene adzakhululukidwe ku iman.

Pali Iman imodzi yomwe Atumiki "alaihim-us-salawâtu wattaslimât" onse anayifikitsa kwa Ummat wawo. Komabe iwo amasiyana wina ndi mzake mu malamulo awo, nyengo, ndi machitidwe achipembedzo.

Palinso mitundu iwiri ya iman: iman-i-khilqi, ndi iman-i-kasbi.

Iman-i-khilqi ndi kapolo obadwa akunena kuti, "Inde," pa nthawi ya ahd-i-misak (pangano lolemekezeka).[1]

Iman-i-kasbi ndi iman yomwe umatengedwa ndi kutsimikizira munthu atatha nsikhu. Iman ya okhulupirira onse ndi chimodzimodzi. Koma zimasiyana amal.

[1] Onani ndime yachitatu ya mutu woyamba wa bukhu la The Rising and the Hereafter.

Iman ndi fardh-i-daim (yokakamizidwa nthawi zonse), pomwe amal imakhala fardh (yokakamizidwa) nthawi yake ikafika.

Iman ndi fardh kwa osakhulupilira komanso kwa Asilamu. Amal ndi fardh kwa Asilamu okha.

Komanso, pali magulu asanu ndi atatu (8) a iman:

Iman-i-matbu ndi iman ya Angelo.

Iman-i-masum ndi Iman ya Atumiki.

Iman-i-maqbul ndi Iman ya okhulupirira.

Iman-i-mawquf ndi iman yokhala ndi zosokonekera ya anthu a bidah

Iman-i-merdud ndi iman ya chiphamaso yomwe munafiq amadzinyenga kukhala nayo.

Iman-i-taqlidi ndi iman ya anthu omwe ayimva kuchokera kwa makolo awo koma sanaphunzire kwa aphunzitsi a za chipembedzo ndipo iman ya anthu awa ndi yosadalilika.

Iman-i-istidlali ndi iman ya munthu amene amadziwa Mawla-imute'ali pofotokoza za kukhalapo Kwake kuchokera ku umboni. Mtima wa munthu uyu ndi wodabwitsa.

İman-i-haqiqi. Munthu amene ali ndi Iman imeneyi sangamukane Mbuye wake (Allahu ta'âlâ) ngakhale zolengedwa zina zonse zitasonkhana pamodzi ndi kugwirizana zomukanira Mbuye wawo (Allahu ta'âlâ) ndipo sangakhale ndi chikayiko chilichonse ngakhale kochepe mu mtima mwake. Monga tanenera poyamba paja, mtundu wa iman uwu ndi wolemekezeka kuposa mitundu yonse.

Iman imachinjiriza ku zinthu zitatu:

Choyamba, imateteza khosi la munthu (kapena moyo wake) ku lupanga.

Chachiwiri, imateteza chuma cha munthu ku (misonkho yotchedwa) jizya ndi kharaj.

Chachitatu, imapulumutsa thupi la munthu ku Jahannama ya muyaya.

"**Aamantu billah ...,"** imatchedwanso Sifat-i-iman kapena muminun bih kapena dhat-i-iman kapena asl-i-iman, chifukwa cha ukulu ndi ulemelero wake. (Kumeneku ndiko kufotokoza kwa nsichi za chikhulupiliro za Chisilamu ndipo kumawerengedwa motere: **"Aamantu billah wa Malaykatihi wa Kutubihi wa Rusulihi wal Yawmil aakhir wabil Qadari khayrihi wa sharrihi min-Allah ta'âlâ wal ba'athu**

ba'adal mawt haqqun. Ash-hadu an laa ilaaha illallahu wa ash-hadu anna Muhammadan Abduhu wa rasuuluhu.")

Iman ili ndi madar awiri, izi ndi nthawi zomwe ndi zokakamizidwa (kwa munthu) kukhala ndi iman: Pa nthawi yomwe munthu wafika msinku wakutha kusankha ndikuzindikira chomwe akuchita ndi pa nthawi yomwe watha nsinkhu.

Ndipo, pali zifukwa ziwiri za iman: Kulengedwa kwa zolengedwa zonse ndi kuvumbulutsidwa kwa Qur'an al-kerim.

Komanso, **pali mitundu iwiri ya umboni**: Delil-i-'aqli (umboni wochokera mukuganiza pogwiritsa ntchito ubongo) ndi delil-i-naqli (umboni ochokera mmabuku ndi otumikira chipembedzo).

Ndiponso, **iman ili ndi rukn** (nsichi) **ziwiri**, **asls** (chiyambi): Ikrar-un bi-l-lisan (kuvomereza ndi lirime) ndi tasdiq-un-bil-janan (kutsimikizira mu mtima).

Ndipo pali zinthu zofunika ziwiri: Kusakhala ndi chikayiko kapena kujejema mu mtima. Ndi kuzindikira chomwe lirime lako likunena.

Koma kodi iman ndi cholengedwa? Tikatengera kuti iman ndi hidayet (chiwongoko) chochokera kwa Allahu adhîm-ush-shân, ndiye kuti siyingakhale cholengedwa. Koma mbali ina ndi cholengedwa, Tikatengera kuti imapezeka chifukwa cha kutsimikiza ndi kunena poyera kwa kapolo wokhulupirira yemwe ali cholengedwa.

Kodi iman ndi gulu, chinthu chimodzi kapena ndi zochuluka? Mu mtima Imani ndi Gulu koma mziwalo imakhala yochuluka.

Yaqeen, kutanthauza chitsimikizo ndi kudziwa Dhat ya Allahu adhîm-ush-shân ndi Kamal (ungwiro Wake).

Khawf, kutanthauza kumuwopa Allahu adhîm-ush-shân.

Raja kutanthauza kusataya chiyembekezo cha Rahmat (Chifundo) cha Allahu adhîm-ush-shân.

Muhabbatullah kutanthauza kukhala ndi chikondi mwa Allahu ta'âlâ Mtumiki Wake "sallallâhu alaihi wa sallam" ndi chikhulupiliro cha Chisilamu ndi okhulupilira.

Haya kutanthauza kukhala wa manyazi pamaso pa Allahu ta'âlâ ndi Mtumiki Wake"sallallâhu alaihi wa sallam".

Tawakkul kutanthauza kudalira mwa Allahu ta'âlâ pa zonse. Kudalira mwa Iye pamene ukuyamba kuchita china chirichonse.

Ndi chani chimatchedwa Iman, Chisilamu, ndi Ihsan?

Iman imatanthauza kukhulupirira mfundo zonse zomwe Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" anasanthula ndi kufotokoza**.**

Chisilamu chimatanthauza kuchita malamulo a Allahu adhîm-ush-shân ndi kupewa zomwe Waletse IYE.

Ihsan kutanthauza kugwira ntchito zopembedza mwadongosolo monga ngati kuti ukumuona Allahu ta'âlâ.

Iman tanthauzo lake la kuchiyankhulo ndi "chitsimikizo chabwino". M'Chisilamu zikutanthauza kukhulupilira ndi kutsimikizira mfundo zisanu ndi imodzi zovomerezeka.

Ma'rifat amatanthauza kumudziwa Allahu ta'âlâ kuti ndi Iye yekha yemwe ali ndi zizindikiro za Kamal (ungwiro) komanso ali kutali ndi makhalidwe opanda ungwiro.

Tawhid ikutanthauza kukhulupilira mu umodzi wa Allahu adhîm-ush-shân osati kumuphatikiza Iye ndi zina.

Chisilamu (Ahkam Al-islamiyya) kutanthauza malamulo ndi zoletsedwa ndi Allahu ta'âlâ.

Din wa millat kutanthauza zikhulupiriro za m'chikhulupiliro mpaka imfa.

Ndiponso iman imatetezedwa mkati mwa zipupa zisanu:

1- Yaqeen (Chitsimikizo)

2- Ikhlas (mowona mtima)

3- Kuchita zinthu za fardh ndikupewa zoipa.

4- Kutsatira Sunnah.

5- Kukhazikika pa adab (khalidwe labwino) ndi kuonetsetsa kuti zikhale chomwecho.

Onse okhazikika m'zipupa zisanu zimenezi adzakhalanso okhazikika mu iman yawo. Kunyalanyaza chimodzi mwa zipupa zimenezi kudzachititsa kuti adani apambane. Munthu ali ndi adani anayi: gulu loyipa kudzanja la kumanja, zilakolako (zokhumba) za nafs kudzanja la ku manzere, kukonda dziko pa tsogolo ndi satana amatseka kumbuyo mwake. Adani anayiwa amapikisana pochotsa iman ya munthu. Gulu loyipa si anthu omwe amabera munthu katundu, ndalama, ndi zina za mdziko okha ayi. Gulu loyipa kwambiri ndi amene amayesetsa kuononga chikhulupiliro cha munthu, iman, adab, haya (kupanda manyazi), ndi mbiri yabwino. Potero amaononga chisangalalo cha munthu pa dziko lapansi pano komanso chisangalalo chake chamuyaya pa tsiku lomaliza. Allahu ta'âlâ ateteze Iman yathu ku zoyipa za adani otere. Ndipo atiteteze ku kusochera kokonzedwa ndi adani a Chisilamu.

Tanthauzo lodalitsika la **Kalima-i-Tawhid**, kunena kuti, **"La illaha illallah"** ndi kuti: Palibe wina aliyense woyenera kumpembedza koma Allahu ta'âlâ yekha. Nthawi zonse amakhalapo ndipo ndi Mmodzi. Iye alibe sherik (mnzake ophatikana naye mu Umulungu wake) kapena nadhir (ofanana naye). Sachingidwa ndi nthawi kapena malo.

"**Muhammadun rasulullah**" kutanthauza kuti Hadrat Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" ndi kapolo wobadwa komanso Mtumiki weniweni wa Allahu ta'âlâ. Ndife Ummat wake, alhamdu-lillah.

Komanso Kalima-i-Tawhid ili ndi mayina asanu ndi atatu:

1- Kalima-i-Shehadat.
2- Kalima-i-Tawhid.
3- Kalima-i-Ikhlas.
4- Kalima-i-Taqwa.
5- Kalima-i-Tayyiba.
6- Da'wat-ul-Haqq.
7- Urwa-t-ul-wuthqa.
8- Kalima-i-themerat-ul-Jannat.

Ikhlas[1] kuti ikwaniritsidwe pafunika izi: Kuchita niyyah (kutsimikiza), kudziwa tanthauzo lake, ndi kuyiwerenga kapena kunena pa mtima mmene ulemelero wake uyenera kukhalira.

Kuchita dhikr kumafuna zinthu zinayi: Tasdiq (kusimikiza), ta'dhim (kuyamika ndi kupembedza), halawat (kukometsera), ndi hurmat (ulemu).

Munthu yemwe wasiya tasdiq ndi munafiq (wachinyengo); munthu yemwe wasiya ta'dhim ndi wa bidah (wowonjezera); munthu yemwe wasiya halawat ndi kapirikoni, amangodzionetsera; kuasiya hurmat ndi fasiq kumayambitsa kusakhulupilira.

Ndiponso pali mitundu itatu ya dhikr:

1- Dhikr-i-awam.
2- Dhikr-i-khawas.
3- Dhikr-i-akhas.

Dhikr-i-awam ndi dhikr ya anthu osaphunzira. Dhikr-i-khawas ndi dhikr yopangidwa ndi akatswiri ozama pa maphunziro a Chisilamu, ndipo Dhikr-i-akhas ndi dhikr ya Atumiki.

[1] Kuchita chinthu chabwino chifukwa Allahu ta'âlâ walamula kapena kuchivomereza ndi kupewa choyipa kapena chauchimo chifukwa chakuti Allahu ta'âlâ Wachiletsa kapena kuchikana.

Ndiponso, pali ziwalo zitatu za munthu zopanga dhikr:

1- Dhikr yopangidwa ndi lilime, kutanthauza kunena Kalima-i-shahadat.

2- Kupanga tawhid ndi tasbih, ndi kuwerenga (kapena kulakatula pa mtima) Qur'an al-kerim.

3- Dhikr yopangidwa ndi mtima.

Pali mitundu itatu ya ma dhikr opangidwa ndi mtima:

1- Kusinkhasinkha umboni ndi zizindikiro zoongolera ku makhalidwe Allahu ta'âlâ.

2- Kusinkhasinkha umboni wa Ahkam Al-islamiyya.

3- Kusinkhasinkha umboni wa zinsinsi za zolengedwa.

Akatswiri a Tafsir akufotokoza za ayat-i-karima ya zana limodzi ndi makumi asanu ndi mbambu ziwiri (152) ya Surah Baqara motere: Qur'an al-kareem ikunena kuti: **"E inu akapolo Anga! Ngati mundichitira dhikr** (kundilemekeza) **pomvera malamulo angat**, **Ine ndidzakulemekezani pokukhululukirani. Ngati mundilemekeze (dhikr) mopempha ndi mapemphero, Ine ndidzakulemekezani m'njira ya Ijabat** (pokupatsani zopempha zanu). **Ngati mungandilemekeze mwa kundichitira ta'at, Ndidzandilemekezani ndi Na'im yanga** [Mparadiso]. **Ngati mundilemekeza muli malo anokha, ndiye kuti ndidzakulemekezani pa Mahshr** (bwalo la milandu pa tsiku lomaliza). **Ngati mungandilemekeze nthawi ya umphawi, ndiye kuti ndidzakulemekezani ndi thandizo langa. Ngati mungandilemekeze m'njira ya** Ijabat (poyankha malangizo anga)**, ndidzakulemekezani m'njira ya hidayat** (chiwongoko). **Ngati mundilemekeza m'njira ya siddiq ndi ikhlas** (m'choonadi ndi mowona mtima)**, ndiye kuti ndidzakulemekezani ndi najat** (chipulumutso). **Ngati mundilemekeza mwa Fatiha-i-sherifa ndi rububiyyat mu Fatiha-i-sherifa, ndiye kuti ndikulemekezani ndi Rahmat** (chikhululuko)**.**"

Akatswiri ophunzira mozama za Chisilamu ananenapo ntchito zokwana zana (100) zochitira dhikr. Tidzanena zina mwa izo:

Msilamu akachita dhikr, Allahu ta'âlâ amakondwera naye ndipo Angelo nawo amakondwera naye koma Satana amadandaula. Mtima wa munthuyo umakhala wofewa ndi wodekha. Amachita mapemphero mwa chifuniro chake komanso mokondwera. Dhikr (kulemekeza Allahu ta'âlâ) kumachotsa madandaulo m'mitima yawo ndi kusangalatsa mitimayo. Kuchita dhikr kumawalitsa nkhope zawo ndi nur. Munthu wopanga dhikr amakhala wolimba mtima ndipo

adzapeza muhabbatullah (chikondi cha Allahu ta'âlâ). Khomo lochokera ku ma'rifatullah (kudziwa Allahu ta'âlâ) lidzatsegulidwa kwa iwo, kuti alandire fayz (ufulu) kuchokera kwa Awliya. Amakongoletsedwa ndi akhlaq-i-hamida (Makhalidwe a bwino otamandika) makumi asanu ndi limodzi.

"Ash-hadu anna Muhammadan 'abduhu wa Rasuluh." Tanthauzo lodala la chiganizo ichi ndi loti: Hadrat Muhammad Mustafa "sallallâhu alaihi wa sallam", Mtumiki wa nthawi ya makono, yemwe anabadwa ngati kapolo koma ndi kudzakhala Mtumiki (Mthenga) wa Allahu adhîm-ush-shân.

Amadya, amamwa ndipo anakwatira. Anali ndi ana amuna ndi akazi. Onse anali ochokera kwa Hadrat Khadija "radiyallâhu 'anhumâ". Ibrahim yekha ndi amene anabadwira kwa Jariya wotchedwa Mariya. Ndipo anamwalira akuyamwabe. Ana ake onse, kupatula Fatima "radiyallâhu 'anhumâ", anamwalira iye mwini asanamwalire. Anamukwatitsa kwa Hadrat Ali karram- Allah ta'âlâ. Hadrat Hasan ndi Hadrat Huseyn ndi ana a Hadrat Ali ndi Hadrat Fatima "radiyallâhu 'anhumâ". Hadrat Fatima ndiye wa pamwamba kwambiri mwa ana ake onse akazi. Ndipo iye anali wokondedwa wa Hadrat Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam".

Rasul-i-akram "sallallâhu alaihi wa sallam" ali ndi akazi odalitsidwa khumi ndi mmodzi: Hadrat Khadija, Sawda, 'Aisha, Hafsa, Umm-i-Salama, Umm-i-Habiba, Zaynab bint -i-Jahsh, Zaynab bint-i-Huzayma, Maymuna, Juwayriyya, Safiyya "radiyallâhu 'anhumâ".

Kitab, Sunnah, Ijma'-i-Ummat, ndi Qiyas-i-mujtahid zimapanga **Adilla-i-shar'iyya**. Akatswiri a Chisilamu amagwiritsa ntchito magwero anayi awa pofuna kuzama pa za chisilamu. 'Kitab (Bukhu)' ndi Liu la Allahu ta'âlâ. "Sunnah" ikuyimira zinthu zitatu zomwe ndi Qawl-i-Rasul (Zoyankhula za Mtumiki wa Allahu ta'âlâ), Fi'li-Rasul (Zochita ndi khalidwe la Mtumiki wa Allahu ta'âlâ), ndi Taqriir-i-Rasul (zomwe anazitsimikizira ndi kuvomereza Mtumiki wa Allahu ta'âlâ). Ijma'-i-Ummat ndi zomwe ma mujtahid (akatswiri a malamulo) okhala m'zaka zofanana anagwirizana, monga Ashab-i-kiram "radiyallâhu 'anhumâ", ndi Madhhab anayi. Qiyas ndi yankho lopezeka pofanizira mfundo ziwiri zomwe ma mujtahid akusiyana.

Tikati Madhhab mchiyankhulo ndi njira. Tili ndi njira ziwiri zosiyana: njira yathu ya i'tiqad (chikhulupiliro), ndi njira yathu ya amal (machitidwe a ntchito).

Imam wathu, wotitsogolera m'njira ya i'tiqad ndi Abu Mansur Maturidi "rahima-hullâhu ta'âlâ" . Njira yake imatchedwa **Ahl as-**

Sunnah. Mtsogoleri wathu pa njira ya amal ndi Imam azam Abu Hanifa “rahima-hullâhu ta’âlâ”. Njira ya iye ndi ya **Madhhab a Hanafi**.

Dzina la Abu Mansur Maturidi ndi Muhammad, dzina la atate ake ndi Muhammad, dzina la agogo ake ndi Muhammad, ndipo dzina la mphunzitsi wake ndi Abu Nasr-i-Iyad “rahima-hullâhu ta’âlâ”.

Dzina la mphunzitsi wa Abu Nasr-i-Iyad ndi Abu Bakr-i-Jurjani, yemwe dzina la mphunzitsi wake ndi Abu Suleyman Jurjani, yemwe aphunzitsi ake ndi Abu Yusuf ndi Imam-i-Muhammad Shaybani. Ndipo mphunzitsi wa aphunzitsi awiriwa ndi Imam a’zam Abu Hanifa “rahima-hullâhu ta’âlâ”. Nchifukwa chake, Imam a’zam ndiye wamkulu wotsogolera Madhhab athu mu I’tiqad ndi mu Amal (m’chikhulupiliro ndi m’machitidwe a ntchito zathu).

Asilamu onse ali ndi ma Imam (atsogoleri) atatu; ndikofunika kuwadziwa. Imam wathu pa malamulo ndi zoletsedwa ndi Qur’an al-Karim. Imam wotidziwitsa za Chisilamu, ndi Hadrat Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam“. Imam wathu yemwe amaonetsetsa kuti lamulo likugwira ntchito ndi mtsogoleri wa dziko wa Chisilamu m’malo mwa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”.

Dzina la mphunzitsi wa Imam a’zam ndi Hammad, yemwe anaphunzitsidwa ndi Ibrahim Nehai, yemwe mphunzitsi wake anali Alqama bin Qays. Alqama bin Qays anali malume wake wa Hadrat Nehai. Mphunzitsi wa Hadrat Alqama ndi Abdullah ibni Mes’ud “rahima-hullâhu ta’âlâ”, yemwe analandira kuzindikira kuchokera kwa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”.

Rasulullah “alaihim-salâm”, analandira kuzindikira kwake kuchokera kwa Jebrail “alaihim-salâm”. Ndipo Jebrail “alaihim-salâm” m’malo mwake adalamulidwa ndi Hadrat Allahu ta’âlâ.

Allahu ta’âlâ wapereka mphatso zinayi za mtengo wapatali kwa anthu: ‘Aql (maganizo, nzeru, kulingalira), Iman, Haya (manyazi), ndi Fi’l, yomwe ndi ‘amal-i-Saalih (Ntchito zachipembedzo).

Kuti mapemphero komanso ntchito zopembedza zilizonse zilandiridwa, izi ziyenera kukwaniritsidwa kaye: Iman, Ilm, Niyyat, Khulus (kuchita moona mtima), kusapwanya ufulu wa ena, (omwe amatchedwa maufulu a quls). Choyamba, munthu ayenera kukhala ndi chikhulupiliro mu Ahl as-Sunnah ndi kudziwa zoyenera kukwaniritsa kuti kpembedza kuchitike bwino.

[Pali kusiyana pakati poti Amal ndi sahih (yowona) ndi kuti yalandilidwa. Machitidwe opembedza ali ndi zifunika zawo ndi ma fardh oti akwaniritsidwe kuti zikhale sahih (zovomerezeka). Ngati

imodzi mwaizo itasowa, kulambirako sikukhala Sahih. Kudzakhala ngati kulambirako sikunachitike. Ndipo munthu sadzakhululukidwa ku chilango chopatsidwe kwa munthu yemwe sanalambire. Ndipo palibe chilango chifukwa cha kulambira komwe kuli sahih ngakhale kuti sikunalandilidwe. Koma msilamu sangapeze thawab (malipiro apadera) pa kulambira kwake komwe sikunalandilidwe. Kuti kupembedza kulandilidwe, kuyenera kuti kukhale kaye sahih. Ndipo zifunika zomwe tafotokozazi ziyenera kukwaniritsidwa. Ufulu wa quls, (omwe tafotokoza kale) zaphatikizidwa mu zifukwa zimenezi.] Imam Rabbani "rahima-hullâhu ta'âlâ" akunena motere mkalata ya makumi asanu ndi atatu ndi mphambu zisanu ndi ziwiri (87) m'bukhu lachiwiri la **Maktubat**):

"Ngati munthu achita ntchito yofanana ndi ya Mtumiki koma ndi kuphinja ufulu wa ena ngakhale pang'ono, sangalowe ku Mparadiso pokhapokha ataubwezera." [Mapemphero ake sadzalandiridwa.]

Ibni Hajar-i-Mekki "rahima-hullâhu ta'âlâ" akuyankhula motere pamene akufotokoza za chimo la zana limodzi ndi makumi asanu ndi atatu ndi mphambu zisanu ndi ziwiri (187) m'buku lake lotchedwa **Zewajir**: Ayat-i-karim 188 m'surah ya Baqara ikuti: "**Ndipo musadye chuma chanu pakati panu mwachinyengopochipereka kwa oweruza (m'njira ya ziphupu)**". Tanthauza la **m'jira ya ziphupu** ndi chinyengo m'njira ya chiwongoladzanja, njuga, kulanda, kuba, kunama, chiwembu, umboni wonama, ndi bodza. Ma Hadith-i-sherif ena amawerenga motere: "**Msilamu amene amadya za halal ndi kuchita zinthu za fardh ndi kupewa za haram komanso osatsautsa anthu ena adzakalowa ku Mparadiso"** ndipo "**Thupi lodyetsedwa za haramu lidzakaotchedwa ndi moto**" ndiponso "**Ngati anthu sali otetezeka ku zonyansa ndi zoyipa za munthu, munthu ameneyo sadzapeza phindu lirilonse kuchokera m'chikhulupiriro chake kapena mapemphero a Namaz kapena Zakaat yomwe apereka"** komanso "**Ngati jilbab (mkanjo) womwe munthu wavala ndi yopeza m'njira ya Haram, Namaz imene wachita atavala mkanjowo siidzalandiridwa."** Hadith-i-sherif yomwe akuyigwiritsa ntchito posanthula tchimo la mazana awiri (200) ikuti: **"Munthu amene amagulitsa malonda a chinyengo sali ndi ife. Malo ake ndi ku Jahannama.** Zanenedwa m'hadith-i-sherif pokambirana za uchimo wa mazana awiri ndi khumi (210) kuti: **"Jahannam ndi malo a munthu amene amasautsa anthu oyandikana nawo ndi lirime lake, ngakhale kuti amachita namaz, amasala kudya ndi kupereka kwambiri sadaka."** Ngakhale oyandikana nawo ali osakhulupirira, nkofunika kuti tisawamvetse kuwawa, achitireni

zabwino, ndi kuwachitira chifundo. Zanenedwa mu Hadith-i-sherif pa chimo la mazana atatu ndi khumi ndi mphambu zitatu (313): **"Munthu amene wapha kafiri mopanda chilungamo pa nthawi ya mtendere, sakalowa ku Mparadiso**". Hadith-i-sherif ina imati: **"Pamene Asilamu awiri akumenyanirana zinthu za dziko, wophedwa ndi wakuphayo onse adzapita ku Jahannama."** Zanenedwanso mu hadith-i-sherif pa utchimo wa mazana atatu ndi khumi ndi mphambu zisanu ndi ziwiri (317): "**Munthu amene akuchitira nkhanza ena, adzazunzidwa nazo pa tsiku lomaliza**.

Izi ndi chimodzimodzi kuchitira nkhanza kwa omwe sali Asilamu. Mu Hadith-i-sherif pa za utchimo wa mazana atatu ndi kumi ndi chisanu (315): **"Pali anthu atatu omwe kupempha kwawo ku dzalandiridwa ndithu: Woponderezedwa**, **mlendo ndi makolo**. Ndipo mu hadith inanso ikuti: **"Pempho la munthu wolakwidwira (woponderezedwa) silidzakanidwa ngakhale atakhala wosakhulupilira."** Mu hadith-i-sherif pa chimo la mazana anayi ndi mphambu ziwiri (402): "**Munthu amene wapha mnzake sali ndi ife, ngakhale kuti nzakeyo atakhala kafiri."** Mu hadith-i-sherif pa chimo mazana anayi ndi makhumi asanu ndi mpambu zinayi (454): "**Mwa machimo onse, chimo lowukira boma lako, chilango chake chimaperekedwa mofulumira kwambiri.** Awa ndi mapeto akumasulira kwathu kuchokera m'bukhu la **Zewajir**. O Asilamu! Ngati mukufuna kupeza chisomo cha Allahu ta'âlâ ndipo kuti mapemphero anu alandiridwe, sungani m'mitima mwanu Hadith-i-sherif zomwe tazitchula pamwambazi! Musaononga chuma, moyo, kapena kudzisunga kwa munthu wina aliyense. Asilamu ndi osakhala asilamu omwe! Osalakwire aliyense! Apatseni anthu ufulu wawo! Ndi ufulu anthu ndi zolengedwa kuti mwamuna apereke 'mahr' kwa mkazi amene wamusudzula. Ngati sapereka, adzalandira chilango chokhwima pa dziko lapansi ndi pa tsiku lomaliza. Ufulu wofunikira kwambiri mwa maufulu a anthu ndi zolengedwa womwe umabweretsa chilango chokhwima (ukaphwanyidwa), ndi kusiya kuphunzitsa abale ako Chisilamu, maka amene ukusunndi ku wasamala. Ngati munthu ataletsa iwo ndi anthu ena kuphunzira Chisilamu ndi kuchita mapemphero awo mozunzika ndi chinyengo, zidzatsimikizika kuti munthuyo ndi wosakhulupilira ndipo ndi mdani wa Chisilamu. Mwachitsanzo kuyipitsa ziphunzitso za Ahl as-Sunnah ndi khalidwe lopanda chipembezo. Iyi ndi njira yomwe anthu a bid'ah ndi opanda Madhhab amatsata poyankhula mau achiwembu ndi kulemba nkhani zoukira. Musalimbane ndi boma kapena malamulo. Lipirani misonkho. Ndi khalidwe la utchimo kuwukira boma, kaya

likhale la nkhanza kapena fasiq (opwanya malamulo a chisilamu). Zalembedwa m'buku lotchedwa **Beriqa**, (lomwe linalembedwa ndi Muhammad bin Mustafa Hadimi "rahima-hullâhu ta'âlâ", yemwe anamwalira mu 1176) [1762 AD], Hadim, Konya ku Turkey.) Ngakhale mukukhala ku dar-ul-harb (m'dziko lolamulidwa ndi anthu osakhulupilira), musaphwanye malamulo ndi ndipo musadelere mphamvu zawo! Musayambitsa fitna (kuukira kwa mpatuko)!

Musamapange ubwenzi ndi anthu owukira Chisilamu, a bidah, kapena anthu omwe sakhulupirira Madhhab onse anayi! Musawerenga mabuku kapena manyuzipepala awo! Musaonere ma pulogalamu awo a pa wailesi kapena kanema m'nyumba zanu! Chitani Amr-i-ma'ruf, (kuphunzitsa Chisilamu) kwa anthu omwe angakumverani! Perekani malangizo mukumwetulira ndi mawu okoma! Onetsani khalidwe labwino, ukulu ndi ulemu wa chipembedzo cha Chisilamu kwa anthu onse okuzungulirani!

Ibni Abidin[1] "rahima-hullâhu ta'âlâ" akunena motere m'gawo loyamba: "Saw'atayn (maliseche ndi mmalo onse ozungulira) ndi awrat (malo achinsinsi) m'Madhhab onse anayi. Ndi fardh m'Madhhab onse anayi kuphimba malo a chinsinsi. Aliyense yemwe saona kufunika kophimba malo a chinsinsi ndi wosakhulupilira. Mamuna yemwe akuonetsa mawondo apangidwe Amr-i-ma'ruf (alangizidwe kuti aphimbe maondo ake). Koma Amr-ima'ruf, ichitike ndi mawu ofewa. Ndipo ngati angayankhe mwamakani inu yankhani mwamtendere. Dzudzulani amuna okakamira kuonetsa ntchafu zawo. Munthu wowonetsa maliseche akuyankha mwaukali (ku uphungu wanu), kadandauleni ku bwalo la milandu kuti akakamizidwe kwapulidwa kapena ku tsekeredwa m'ndende. Komanso ndi chimo kuyang'ana maliseche a munthu." Ndi fardh m'Madhhab onse anayi kuti akazi aziphimba matupi awo onse kupatula manja ndi nkhope zawo kwa amuna omwe ali na-mahram kwa iwo ndi kwa akazi omwe sali Asilamu. Madhhab a Shafi'i, amalamula kuti ndi fardh kwa akazi kusaonetsa nkhope zawo (kwa anthu amene tawatchulawa). Ngati iwo, atate awo kapena amuna awo salilemekeza lamuloli, adzakhala osakhulupilira. Ndi tchimo lalikulu anyamata kuvina kapena kusewera

[1] Katswiri wa maphunziro a Fiqh, yemwe dzina lake lenileni ndi Sayyid Muhammad Emin bin 'Umar bin 'Abd-ul-'Aziz yemwe anabadwa mu 1198 [1784 A.D.],ndi kumwalira ku Damascus mu 1252 [1836]. Analemba bukhu la magawo asanu lotchedwa **Radd-ul-muhtar** kutambasula mwatsatanetsatane bukhu lotchedwa **Durr-ul-mukhtar**, lomwenso linalembedwa ndi 'Ala-ud-din Haskafi "rahima-hullâhu ta'âlâ" yemwe anabadwa mu 1021 ku Haskaf ndikumwlira mu 1088 [1677]). Zambiri mwa

ntchafu za miyendo yawo ziri pa mtunda. Komanso ndi tchimo kwa atsikana kusaphimba mitu ndi manja awo pochita masewero. Ndi tchimo kuwonelera anyamata kapena atsikana omwe sanavale mwa malamulo posewera.

Msilamu asataye nthawi yake yopuma posewera kapena kuchita zinthu zopanda pake. Ndi kwa phindu kugwiritsa ntchito nthawi pophunzira ndi kuchita Namaz. Zanenedwa mu **Kimya-i-sa'adat** kuti: "Monga momwe ziliri kuti ndi haram kwa akazi kapena atsikana kutuluka ndi mitu, tsitsi, mikono ndi miyendo yawo ziri poyera, momwemonso ndi haram kwa iwo kutuluka atavala zovala zopyapyala; zovala zozikongoletsa, zothina, ndi zonunkhiritsa. Makolo, amuna awo, kapena azichimwene awo adzakhala nawo m'machimo ngati awalekelera akuchita izi. Nawo adzalandira gawo la mazunzo omwe adzakumane nawo akazi ndi atsikana oterewa." Adzawotchedwa limodzi ku Jahannama. Ngati apanga tawba, adzakhululukidwa ndipo sadzawotchedwa. Allahu ta'âlâ amakonda anthu ochita tawba.

ZAWJAT (AKAZI) NDI GHAZAWAT (MAULENDO) A MTUMIKI
(Akazi Odalitsika ndi Makampeni opatulika a Mtumiki)

Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anali ndi zaka makumi anayi. Mngelo wotchedwa Jebrail anadza kwa iye ndi kumuwuza kuti iye ndi Mtumiki. Patatha zaka zitatu (ali ndi zaka 43), Iye analengeza za Utumiki wake ku Makka. Ichi chinali chaka cha **Bi'that**. Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anachita Jihad (nkhondo zopatulika) makumi awiri mphambu zisanu ndi ziwiri. Mwa iye yekha anamenya nkhondo zisanu ndi zinayi (9). Mu nkhondo zopatulika khumi ndi zisanu ndi zitatu (18), iye anali wotsogolera nkhondo.

Anali ndi ana asanu ndi atatu (8) amuna anayi, akazi anayi. Anali ndi akazi khumi ndi mmodzi (11). Kwa bambo ake, anali ndi amalume khumi ndi awiri (12) ndi azakhali asanu ndi mmodzi (6). Anali ndi zaka makumi awiri ndi zisanu (25) pomwe anapanga nikah ndi Khadija-tul-kubra. Patapita chaka chimodzi Khadija-tul-kubra atamwalira Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ali ndi zaka makumi asanu (50). Iye anapanga nikah ndi Aisha mwana wa Abu Bakr "radiyallâhu anh" atalamulidwa ndi Allahu ta'âlâ. Ndipo anamwalira ali ndi zaka makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zitatu (63). Anamwalilira mchipinda cha Aisha, chomwe chinali choyandikana ndi Masjid Nabi. Anayikidwa

mchipinda momwemo. Abu Bakr ndi Umar “radiyallâhu ’anhum” nawonso anayikidwa mchipinda chomwechi. Pamene Masjid inali kukulitsidwa, chipindacho chinaphatikizidwa ku Masjid. Mu chaka cha chisanu ndi chiwiri (7) cha Hijira, anapanga nikah ndi Umm-i-Habiba, yemwe adali mwana wa Abu Sufyan bin Harb. Abu Sufyan anali mkulu wa anthu osakhulupilira achi Quraish ku Makka. Abu Sufyan ndi bambo wa Mu’awiya “radiyallâhu ’anhumâ”. Anakhala okhulupilira mzinda wa Makka utagonjetsedwa. Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anapanga nikah ndi Hafsa, yemwe anali mwana wamkazi wa Umar “radiyallâhu ’anhumâ”.

M’chaka cha chisanu cha Hijira, Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anamugula kapolo yemwe anagwidwa kuchokera ku fuko la Beni Mustalaq. Dzina lake anali Juwayriya ndipo anagwidwa pa nkhondo yopatulika ya **Mureysi**. Juwayriya anali mwana wa mkazi wa mfumu. Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anamupanga kukhala mfulu ndikupanga naye nikah. Pofuna kulimbikitsa za chipembedzo adapanga nikah ndi Umm-Salama, Sawda, Zaynab binti Huzayma, Maymuna, and Safiyya “radiyallâhu ’anhumâ”. Koma nikah yake ndi Zaynab, mwana wamkazi wa amalume ake, inapangidwa ndi Allahu ta’âlâ.

Mu umoyo wake anayenderedwa ndo Jebrail “alaihim-salâm” maulendo zikwi makumi awiri ndi zinayi (24,000). Anatengedwa pa ulendo wopita kumwamba ali ndi zaka makumi asanu ndi chimodzi (51) za kubadwa mu 621 AD. Ulendo uwu umatchedwa Mi’raj. Anasamuka ku Makka kupita ku Medina ali ndi zaka makumi asanu ndi ziwiri (52) mu 622 AD. (Nsamuko umenewu umatchedwa Hijra.) Iye ndi Abu Bakr anakhala m’phanga la phiri la Sawr kwa usiku utatu (3). Kuphangako anachoka chakumathero a usiku wa Lolemba. Atayenda kwa sabata imodzi, anafika ku Kuba, mmudzi wa Madina, pa 20 September ndipo linali Lolemba. Ndipo Lachisanu lotsatiralo pa 24 September ndi pamene analowa ku Madina.

Nkhondo yopatulika ya Badr inamenyedwa mchaka cha chiwiri cha Hijra, lolemba m’mwezi wodalitsika wa Ramadan. Asilikali a Chisilamu analipo mazana atatu ndi khumi ndi atatu (313), koma asanu ndi atatu (8) mwa iwo sanamenye nawo. Anali pa ntchito zina. Ma Quraysh anali chikwi chimodzi (1,000). Ma Sahabi khumi ndi atatu (13) anafera mnjira ya chikhulupiliro. Abu Jahl ndi osakhulupilira ena makumi asanu ndi awiri anaphedwa.

Nkhondo yopatulika ya Uhud inamenyedwa m’mwezi wa Shewwal m’chaka chachitatu cha Hijira. Asilikali a Chisilamu mazana asanu ndi

awiri (700) ndiwo analimbana ndi gulu la nkhondo lamphamvu la anthu okwana zikwi zitatu (3,000) la ma kafir. Ashab-i-kiram okwana makumi asanu ndi awiri (70) anafera chikhulupiliro. Nkhondo yopatulika ya Uhud itatha ndipo patapita miyezi inayi, anyamata makumi asanu ndi awiri (70) achi Sahabi anatumizidwa ku Najd. Iwo amakagwira ntchito yoyitanira anthu ku Chisilamu. Koma atafika pa malo otchedwa **Bir Mauna**, adani anawabisalira ndipo gulu lonse kupatula ma Sahabi awiri linaphedwa mnjira ya chikhulupiliro.

Nkhondo yopatulika yotchedwa Hendek (Ngalande) inachitika m'chaka cha chisanu cha Hijir. Ma kafir analipo zikwi khumi (10,000) pomwe Asilamu analipo zikwi zitatu (3,000). Ma kafir anauzinga mzinda wa Madina. Asilamu anali atakumba kale ngalande mozungulira mzinda wa Madina.

M'chaka cha chisanu ndi chimodzi, pangano la **Bait-ur-rizwan** linapangidwa pamalo otchedwa Hudaybiya. Nkhondo yopatulika ya Hayber inachitika m'chaka cha chisanu ndi chiwiri. Asilamu anali zikwi zitatu (3,000) ndipo analimbana ndi gulu la nkhondo la mphamvu la Byzantine la a silikali zikwi zana (100,000) . Jafar Tayyar "radiyallâhu 'anh" adafera mnjira ya chikhulupiliro pa nkhondo imeneyi. Khalid bin Walid ndi yemwe anapambana pa nkhondoyo.

Makka inagonjetsedwa m'chaka cha chisanu ndi chitatu (8). **Hunayn** ndi nkhondo yopatulika yodziwika komanso yayikulu. Pa nkhondoyi Asilamu amalimbana makafir a ku Qays ndipo inachitikira mu kwawa la Hunayn. Asilamu anapambapananso pa nkhondoyi. **Hayber** ndi linga lodziwika bwino la Ayuda. Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anatumiza Hadrat Ali, ndipo linga lidagonjetsedwa. Anali malo amenewo omwe Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anapatsidwa chakudya cha poizoni, chimene iye anakana kudya. Pamene anali mnjira kubwelera kuchokera ku nkhondo yopatulikayi, Hadrat Aisha ananamiridzidwa nkhani zomunyozetsa, zomwe zinamumvetsa chisoni kwambiri Mtumiki wa Allahu ta'âlâ. Ayahs inatsika, yomwe inazindikiritsa kuti zonenedwazo zinali za bodza lankunkhuniza. Nkhani ina yodziwikanso kwambiri ndi kupambana kwa nkhondo ya Taif.

Ngati mukufuna chisangalalo, o! mnyamata,
Gwiritsa Chisilamu, mwana wanga, nthawi zonse.

Fardh, wajib, Sunnah, ndi mandub,
Komanso chita amr-i-bi-l-ma'ruf mokwanira.

Zichiteni nthawi zonse, osasiya ngakhale imodzi,
Zazikulu ndi zazing'ono chiodzimodzi, mwangwiro.

Ndikoyeneranso, kupewa makruh ndi haram,
Ufulu wa ma quls uyenera kupewedwa, makamaka.

Phunzirani kuchokera kwa Ahl as-Sunnah!
Chitani zomwe mwaphunzira, nthawi yomweyo!

TSATANETSATANE WA IMAN

Pali zokhulupirira khumi ndi ziwiri za tsatanetsatane wa Iman: Mbuye wanga ndi Allahu ta'âlâ. Umboni wanga wolembedw ndi Surah Baqara, ayah ya zana limodzi ndi makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zitatu (163). Mtumiki wanga ndi Hadrat Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam". Umboni wanga wa m'malembo ndi Surah Al-Fath, ma ayah ya makumi awiri ndi mphambu zisanu ndi zitatu (28) ndi makumi awiri ndi mphambu zisanu ndi zinayi (29). Chipembedzo changa ndi Chisilamu. Umboni wanga m'malemba ndi ayah ya Allahu ta'âlâ ya khumi ndi chisanu ndi chinayi (19) mu Surah Al-Imran. Bukhu langa ndi Qur'an-i-'adhîm-ush-shân. Umboni ndi ayah yachiwiri (2) ya Surah Baqara. Qibla yanga ndi Ka'ba-i-sherif.

Umboni wake ndi Surah Baqara, ayat-i-karima ya zana limodzi makumi anayi ndi mphambu zinayi (144).

Madhhab anga mu i'tiqad (iman) ndi **Ahl as-Sunnah wa-l-jama'at**. Umboni wanga ndi Surah Al-An'am, ayah ya zana limodzi ndi makumi asanu ndi mphambu zitatu (153).

Kholo langa (loyambilira) ndi Hadrat Adam. Umboni wanga ndi Surah Araf, ayah ya zana ndi makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri (172).

Deen yanga ndi deen-i-islam. Umboni wanga ndi ayah ya makumi asanu ndi awiri ndi mphambu zisanu ndi zitatu (78) ya Surah Hajj.

Ine ndi mmodzi wa Ummat wa Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam". Umboni wanga ndi ayah zana limodzi ndi khumi (110) mu Surah Al-Imran.

Ine ndine Mumin (wokhulupilira), haqqan (mu chowonadi). Umboni wanga ndi ayah yachinayi mu Surah Anfal. Al-hamdu lillahi ala-ttawfiqihi wa-s-taghfirullaha min kulli taqsirin.

Ilm (kudziwa kolondola) ndi yokwera kuposa amal (ntchito yolondola) pa zifukwa zisanu: ilm imadzidalira pomwe amal imadalira

ilm. Ilm ndiyofunika pomwe amal siyingayime payokha popanda Ilm. Ilm ingapereke phindu payokha, pamene amal siyingapereke phindu popanda ilm. Mwachidule, simungapange ntchito yolondola popanda kudziwa kolondola.

Ilm ndi yokwera kuposa aql (malingaliro). Ilm ndi qadim (yosatha), pomwe aql ndi hadith (zinakhazikitsidwa mopanda kuchokera mu chinthu china).

Zinat (zozikongoletsera) za mamuna ndi za ikhlas (zoona mtima). Zozikongoletsera zoona mtima zimakhala ndi iman. Zinat ya iman imakhala ku Jannah (Mparadiso). Zinat ya ku Jannah imakhala ndi ma huris (anamwali okongola a ku Jannah), ma ghilman, ndi kuwona Jamalullah, (maonekedwe a Allahu ta'âlâ osatheka kuwazindikira kapena kuwafotokoza).

Amal (ntchito zolondola) zikanakhala gawo limodzi la Iman, mkazi yemwe akusamba sibwenzi akuloledwa kusachita namaz ya tsiku ndi tsiku, popeza iman siyingathe kusiyidwa.

Ndi fardh kunena Kalima-i-shahadah (kosachepera) kamodzi mmoyo wa munthu. Umboni wake uli pa ayah ya khumi ndi chisanu ndi chinayi (19) mu Surah Muhammad.

Ponena Kalima-i-shehadat zinthu zinayi izi ziyenera kukwaniritsa: Kuyankhula moona mtima pomwe monga lilime likuyankhulira. Kudziwa tanthauzo lake. Kunena ndi mtima woona. Kuyinena ndi ta'dhim (kulemekeza, kuchitira ulemu waukulu).

Pali zophindu zokwana zana limodzi ndi makumi atatu (130) pongonena Kalima-i-shahadah. Komabe, zinthu zinayi izi zitha kulepheretsa kupeza zophindulazi.

Zinthu zinayi zimenezi ndi izi: Shirk, shak, tashbih, ndi ta'til. Shirk ndi kumphatikiza Allahu ta'âlâ ndi wina wake kapena china chake mu Umulungu wake.

Shak imatanthauza maks (kupendamapendama) m'chipembedzo. Tashbih ndi kufanizira Allahu ta'âlâ ndi cholengedwa chongoyerekezera. Ta'til kukhulupilira ndi kunena kuti "Allahu ta'âlâ alibe gawo pa zolengedwa ndi kuti chilichonse chimadza pa chokha ikafika nthawi yake."

Mwa ma phindu zana limodzi ndi makumi atatu (130) amene munthu amapeza ponena Kalima-i-shahadah, ma phindu makumi atatu (30) atchulidwa mmawu akudzawa. Ma phindu makumi atatuwo ali motere: asanu mwa iwo umapeza pa dziko lapansi, asanu otsatira umapeza pa nthawi ya imfa, asanu otsatira umakapeza m'manda,

asanu otsatira amapezeka ku Arasat (pa bwalo la milandu), asanu otsatira ndi a ku Jahannama ndipo asanu omalizira ndi a ku Mparadaiso. Ma phindu asanu a pa dziko lapansi ndi awa:

1- Dzina la munthu lidzayitanidwa mokongola

2- Ahkam Al-islamiyya adzakhala fardh (okhazikika) pa munthu

3- Khosi la munthu lidzakhala lotetezeka ku lupanga

4- Allahu ta'âlâ adzakondwera naye munthuyo

5- Okhulupilira onse adzakhala ndi chikondi pa iye

Zotsatira zisanu za phindu pa nthawi ya imfa ndi izi:

1- Azrail "alaihim-salâm" (mngelo wa Imfa) adzabwera kwa iye ali mmaonekedwe okongola.

2- Mngelo amachotsa moyo wa munthu mofewa komanso mosavuta monga ngati mmene mungakokere tsitsi loti liri mmafuta.

3- Fungo lochokera ku Jannah (Mparadiso) lidzafika kumeneko.

4- Moyo wa munthu udzakwera ku Illiyyin (uwu ndi munda wapamwamba pa minda isanu ndi itatu ya Jannah), ndipo angelo adzafika kumeneko ndi nkhani yabwino

5- Liwu lidzati: "Marhaba (Moni!) O okhulupilira! Malo anu ndi ku Jannah.

Zotsatira zisanu za phindu m'manda a munthu wonena Kalima-i-shahadah ndi izi:

1- Manda a munthu adzakhala otakasuka.

2- (Angelo ofunsa otchedwa) Munker ndi Nakir adzabwera kwa munthu m'mawonekedwe okongola.

3- Mngelo adzaphunzitsa munthu pa zomwe sadziwa.

4- Allahu ta'âlâ adzamuuzira munthu zinthu zomwe sakudziwa.

5- Munthu adzaona nyumba yake ku Jannah.

Zotsatira zisanu za phindu pa bwalo la Arasat ndi izi:

1- Kufunsidwa ndi kuwerengeredwa kwa munthu kufotokoza zomwe wakumana nazo kudzakhala kosavuta.

2- Bukhu la zochita za munthu, (kaundula wa zimene munthu anachita ndi kunena m'moyo wake wonse), lidzapatsidwa kwa iye kudzanja la manja lake.

3- Thawabu za munthu zidzalemera kwambiri pa sikelo.

4- Munthu adzakhala pa mthunzi wa Arsh-i-Rahman.

5- Munthu adzaoloka (mlatho wotchedwa) Sirat mofulumira ngati mphenzi.

Zotsatira zisanu za phindu ku Jahannama ndi izi:

1- Ngati munthuyo ati akalowe ku Jahannama, maso ake sadzakhala otuwa ngati anthu ena akumoto.

2- Munthu sadzakangana ndi Satana wake.

3-Sadzamangidwa ndi zingwe zamoto mmanja ndi sadzamangidwa unyolo m'khosi mwake.

4- Munthu sadzamwetsedwa madzi otchedwa Hamim (madzi otentha kwambiri).

5- Sadzakhala ku Jahannama kwa muyaya.

Zotsatira za phindu zisanu ku Jannah ndi izi:

1- Angelo onse adzamupatsa moni.

2- Munthu udzakhala bwenzi la Siddiqs.

3- Jannah idzakhala malo ake amuyaya.

4- Allahu ta'âlâ adzakondwera naye.

5- Munthu adzapeza madalitso ochuluka kwambiri pomuwona Allahu ta'âlâ.

[Qadi-zada Ahmad Efendi (1133–1197 [1783 A.D.]) akunena motere polongosola njira ya chikhulupiliro yotchedwa Faraid-ul-Fawaid: Jahannama ili ndi zigawo zisanu ndi ziwiri (7), imodzi pansi pa ina. Moto wa gulu lirilonse ndi woopsa kwambiri kuposa wa pamwamba pake. Asilamu amachimo osakhululukidwa adzatenthedwa pa gawo loyamba malinga ndi machimo awo; Kenako adzatulutsidwa ku Jahannama ndipo adzatengedwa kupita ku Jannah.

Zigawo zisanu ndi chimodzi zinazo ndi mowotchera osakhulupilira osiyanasiyana. Ma Munafiq adzatenthedwa mu gawo lachisanu ndi chiwiri, lomwe liri ndi chilango choopsa kwambiri. Iwowo ndi osakhulupilira, a nkhope ziwiri, amene m'mawu awo, amachisilira Chisilamu, koma m'mitima mwawo ndi osakhulupilira oyipitsitsa. Osakhulupilira azizati akatenthedwa nkukhala phulusa, Allahu ta'âlâ adzidzakawalenganso kwatsopano ndi kuwa ponyanso kumoto. Izi zidzachitika ndi kudzapitilirabe kwa muyaya. Jannah ndi Jahannam ndi zoti zilipo ndithu.

Malinga ndi kunena kwa akatswiri ena ophunzira a Chisilamu, komwe kuli Jahannama sikudziwika. Koma ena amati ili pansi pa zigawo zisanu ndi ziwiri za nthaka. Kuyankhula uko kukusonyeza kuti Jahannama si ili m'dziko lapansi.

Popeza dziko, dzuŵa ndi nyenyezi zonse zili mu mlengalenga woyamba pomwe dziko tili ifeli pansi pake pali thanka zisanu ndi iwiri.

Choncho, Jahannama iyenera kukhala mu gawo limodzi mwa magawo asanu ndi awiri akumwamba.]

ZOYAMBITSA KUSAKHULUPILIRA (KUFURU)

Kufuru ndi kusagwirizana kapena kukanira malamulo a Allahu ta'âlâ. Ndipo pali mitundu itatu ya Ukafiri: Kufurui-inadi, kufuru-i-jahli ndi kufuru-i-hukmi.

Kufuru-i-inadi ndiko kukana Chisilamu ndi iman mwamakani koma munthuyo akuchita zimenezi modziwa. Mwachitsanzo Kufuru ya anthu monga Abu Jahl, Fir'awn (Farawo), Namrud (Nimrod), ndi Shaddad bin Ad. Choncho ndi zololedwa kunena momveka bwino kuti iwowa ndi anthu akumoto.

Kufuru-i-jehli: Monga momwe anthu osakhulupilira omwe akudziwa kuti Chisilamu ndi chipembedzo chowona, ndipo amamva azan-i-Muhammadi ikuchitika; ukawauza kuti: "Bwerani, khalani Asilamu," iwo amayankha: "Njira ya moyo wathu ndi yomwe tinaphunzira kwa makolo athu akale ndi mabanja awo. Ifenso tidzapitiriza zomwezo."

Kufuru-i-hukmi, kutanthauza tahqir (kuchita chinthu mwa mnyozo) m'malo mwa ta'dhim (kupereka ulemu malinga ndi ukulu wake) ndi ta'dhim m'malo mwa tahqir.

Ndi ukafirinso kuwachitira chipongwe Awliya ndi Anbiya (Atumiki) ndi Ulama (Akatswiri) a Allahu ta'âlâ zonena zawo ndi mabuku awo a Fiqh ndi ma fatwa mmalo mowalemekeza. Komanso, ndi kufuru kukonda miyambo ya chipembedzo cha osakhulupilira ndi kuvala zunnar (lamba wa zingwe amavala wansembe) popanda darurat kutero. Ngakhalenso kuvala chipewa cha unsembe ndi zizindikiro zina za ukafiri monga mtanda.

Kufuru kumadzetsa zovuta zisanu ndi ziwiri (7): Kumachotsa chikhulupiliro ndi nikah. Nyama yophedwa ndi kafiri siyingadyedwe, (ngakhale atapha mogwirizana ndi malamulo onse a Chisilamu). Zochita zake m'banja lake la halaal zimasanduka za chisembwere. Zimakhala wajib kupha munthu ameneyo. Jannah imamutalikira ndipo Jahannama imamuyandikira. Akamwalira ali kafr Janaza yake osazamuchitira namaz.

Ngati munthu alumbira mosakakamizidwa kuti: "Ujeni ndi ujeni ali (kapena alibe) chakuti ndi chakuti; ngati ndikunama ndikhale kafiri," kulumbira kwakeko kumupangitsa kukhala kafiri, osatengera kuti

wanama kapena wanena zoona. Munthu ameneyo akufunika akhonzanso (tejdid) iman ndi nikah yake.

Ndi ukafiri kusilira mchitidwe woletsedwa m'Chisilamu monga dama, katapila ndi bodza, ponena kuti: "Zikanakhala halal bwenzi ndikuchita!"

Ndi ukafiri kukhulupirira Atumiki onse ndi kukaikira za Mtumiki wina. Mwachitsanzo kunena kuti: "Ndimakhulupilira mwa Atumiki alaihimus-salawatu-wat-taslimat, koma sindikudziwa ngati Adamu "alaihim-salâm" ndi Mtumiki." Munthu amene sadziwa kuti Hadrat Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" ndi Mtumiki womaliza, amakhala kafiri.

Akatswiri ena ophunzira a Chisilamu amanena kuti munthu akayankhula mokayikira za Atumiki amakhala kafiri. Mwachitsanzo kunena kuti: "Ngati zimene Atumiki alaihimus-salawatu-wat-taslimat ananena zili zowona, ndiye kuti tapeza chipulumutso." Birgivi "rahmatullâhi 'alaih" akunena kuti: "Ngati munthuyo akunena mosonyeza kukayikira, amakhala kafiri koma ngati akunena choncho mwa ilzam (motsimikizira mtsutso), sakhala kafiri.

Zanenedwa ndi akatswiri ophunzira a Chisilamu kuti ngati munthu wayitanidwa kuti adzachite namaz ndi anzake ndipo iye ndi kukana, iye amakhala kafiri. Komabe, sakhala kafiri ngati akutanthauza kunena kuti: "Sindichita namaz chifukwa choti inu mwandilangiza. Ndichita zimenezi chifukwa Allahu ta'âlâ walamula."

Munthu amakhala kafiri ngati atakanila ma Sunnah a Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anthu atamulangiza monga, mametedwe a ndevu pofuna kutsatira Sunnah ya Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam". Izi zikukhudza chiri chonse cha Sunnah malinga ngati chikudziwika momveka bwino komanso mwa tawatur kuti mchitidwe womwe ukunenedwawo ndi wa Sunnah. Chitsanzo pa izi ndi kutsuka mano ndi Miswak usanayambe kapena pochita Udhu. Hadrat Birgivi[1] akuwonjezera kufotokoza pa mfundo iyi motere: "Kudzakhala kufuru pokhapokha atanena zimenezi motsutsa mchitidwe wa Sunnah koma sikudzakhala kufuru ngati akutanthauza kuti sadzachita chifukwa choti wina wanena koma adzachita chifukwa ndi Sunnah ya Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" [Koma Yusuf Qardawi akunena motere pa tsamba la makumi asanu ndi atatu ndi mphambu imodzi (81) m'buku lake lachinayi lotchedwa **Al-halal wa-l-haram fi-l-islam**:

[1] Zeyn-ud-din Muhammad Birgivi Efendi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (928 [1521 A.D.], Balıkesir – 981 [1573], Birgi, d. of plague).

Hadith-i-sharif yolembedwa m'buku lotchedwa **Bukhari-i-sherif** (kapena **Jami-i-sahih**[1] imati: "**Khalani mosiyana ndi ma mushrik**! **sungani ndevu zanu**, **tsukadulirani masharubu anu!"** Hadith-i-sharif iyi imaletsa kumeta ndevu zanu kapena kumeta mozifupikitsa. Opembedza moto amadulira ndevu zawo. Ena amameta kumene ndevu zao. Hadith-i-sharif iyi ikutilamula kuchita zinthu mosiyana ndi chizolowezi chawo. Akatswiri ena a Fiqh ananena kuti Hadith-i-sharif iyi ikutanthauza kuti ndi wajib kusunga ndevu ndipo ndi haram kumeta ndevu. Mmodzi wa iwo, Ibni Taymiyya, akulemba motsindika kutsutsa zometa ndevu. Koma malinga ndi kunena kwa akatswiri ena ophunzira a Chisilamu, kusunga ndevu ndi mwambo, osati kulambira. Bukhu la Fat-h limagwira mawu a Iyad kuti ndi makruh kumeta ndevu (popanda udhr [chifukwa chololedwa]). Izi ndiye zoona zake. Hadith-i-sharif iyi siyikusonyeza kuti ndi wajib kusunga ndevu. Pakuti, kwanenedwa mu Hadith-i-sharif kuti: "**Ayuda ndi Akhrisitu samasintha mtundu** (kudaya) **wa** tsitsi ndi ndevu zawo. **Chitani zosiyana ndi zomwe amachita!"** Apa, Hadith-i-sharif ikunena kuti dayani tsitsi ndi ndevu zanu. Hadith-i-sharif iyi sikusonyeza kuti ndi wajib kudaya tsitsi ndi ndevu koma ndi mustahab kutero. Chifukwa ena mwa Ashab-i-Kiram amadaya tsitsi ndi ndevu zawo koma ambiri mwa iwo sanachite. Zikanakhala wajib ngati onse akanatero. Chimodzimodzi nkhani ya Hadith-i-sharif yosunga ndevu; ndi mustahab kusunga ndevu, osati wajib. Mwa akatswiri a Chisilamu palibe yemwe anameta ndevu chifukwa unali mwambo wa Asilamu kusunga ndevu mu nthawi yawoyo. Kusatero kunali ngati kunyoza miyambo ya Asilamu –makruh (khalidwe lonyansa). Zidzakhala haram ngati zitayambitsa fitna (kugawikana). Apa tamaliza kumasulira kwathu kuchokera kwa Qardawi. M'mawu oyamba a bukhu lake, Qardawi walemba kuti wasakaniza ziphunzitso za Fiqh za Madhhab onse anayi. Ndipo wati sichilungamo kutsatira Madhhab amodzi okha. Potero iye wapatuka m'njira yotsogozedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunnah, chifukwa akatswiri a Ahl as-Sunnah "rahima-hullâhu ta'âlâ" akunena kuti Msilamu aliyense ayenera kutsanzira imodzi mwa Madhhab anayiwa. Munthu wophatikiza Madhhab adzakhala munthu wa la-madhhabi, zindiq (wapatuka, wopanda madhhab). Komabe, chifukwa mawu Zolembedwa za Qardawi zafotokozedwa apa chifukwa nkhani yake ya ndevu imagwirizana ndi chiphunzitso cha Madhhab a Hanafi. Hadrat 'Abdul-Haqq-i-Dahlawi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (958 [1551 AD] -

[1] Yolembedwa ndi Muhammad bin Isma'il Bukhari "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (194 [810 A.D.], Bukhara – 256 [870], Samarkand).

1052 [1642], Delhi) akunena motere mu bukhu lachitatu la **Eshi'atul-leme'at:**

"Pa nkhani ya tsitsi ndi ndevu, akatswiri ophunzira a Chisilamu amatsata miyambo ya komwe amakhala. Kusatsata miyambo ya malo omwe munthu ukukhala kumayambitsa mbiri yoyipa. Dziwani kuti zomwe ziri mubah (zololedwa) dela lina zitha kukhala makruh (zonyansa) dera lina."

Muhammad bin Mustafa Hadimi "rahima-hullâhu ta'âlâ" (d. 1176 [1762 AD], Hadim, Konya, Turkey) akunena m'bukhu lake lotchedwa **Bariqa** kuti: "Kwanenedwa mu Hadith-i-sharif kuti: **"Fupikanitsani masharubu anu ndipo talikitsani ndevu zanu."** Choncho ndi koletsedwa kumeta ndevu kapena kuyepula kusiya zochepa. Ndi Sunnah kusunga ndevu mpaka zitatalika ngati kutalika kwa bagela. Komanso ndi Sunnah kuzikonza zikatalika kuposa kutalika kwa bagela. Kutalika kwa bagela ndi utali wofanana ndi kuchuluka kwa m'lifupi mwake zala zinayi (pafupifupi 10cm kapena 4 inches) kuyambira kumunsi kwa mlomo wapansi. Sultan akalamula chinthu chomwe chili Sunnah, ngakhale kuti ndi mubah (chololedwa), chimakhala wajib kuchichita. Chinthu choti Sultan akuchichita pamodzi ndi Asilamu onse, chimatanthauza kuti ndi lamulo. Zikatero ndiye kuti ndi wajib kusunga ndevu ndipo kumeta kumatanthauza kusiya chinthu chomwe chili wajib. Ndi kosaloledwa kwa munthu amene wasiya zomwe onse akupanga mdelalo kukhala imam mu msikiti ndi kutsogolera namaz ya jammah. Koma ngati muli ku Dar-ul-harb (nyumba ya nkhondo kapena kuti kumalo komwe simungachite za chisilamu mwa mtendere), ndi kololedwa, tingoti ndikoyenera kumeta ndevu zanu kuopera kuti mungazunzidwe kapena kuchotsedwa ntchito. Izi zingapangise kuti mulephere kupeza zofunika pa moyo wanu kapena kuti muthe kuchita Amr-i-ma'ruf, kutumikira Asilamu ndi Chisilamu, ndi kuteteza chikhulupiliro chanu ndi kudzisungira ulemu wanu. Popanda 'udhr, ndi makruh kudulira kapena kumeta ndevu. Ndipo zili bidah yosatha kukhala ndi ndevu zofupikirapo kuposa kutalika kwa chibagera ndi kukhulupilira kuti potero mukuchita Sunnah. Kutero ndi kusintha Sunnah. Kuchita bid'ah ndi tchimo lalikulu kuposa kupha munthu.]

Tiyeni tiyerekeze kuti achinyamata afika pa msinkhu woganiza bwino mwa wokha ndipo atha msinkhu ndikuchita nikah. Koma iwo ndi kulephera kuyankha funso lokhudza zizindikiro za iman. Izi zingatanthauze kuti iwo sanali Asilamu ndipo nikah ya pakati pawo idzakhala sahih pokhapokha ataphunzitsidwa mfundo za Iman. Ndipo

nikah yawo idzayenera kuchitika mwatsopano. Chonde onani mutu womwe ukunena za ma fardh makumi asanu ndi anayi.

Ngati munthu wadulira masharubu ake ndipo wina amene ali naye ndikunena kuti, “Siziri bwino,” ndikotheka wonenayo iman yake isokonekera. Chifukwa ndi Sunnah kudulira masharubu, ndipo wonenayo wapeputsa zinthu za Sunnah.

Ngati munthu wavala chovala cha siliki chomwe chikuphimba thupi lake lonse kuyambira ku mutu mpaka ku mapazi, ndipo wina ndi kumuwona ndikunena kuti: “Udalitsike nayo,” imana ya woyankhulayo ingawononge ke.

Ngati munthu achita chinthu cha makruh monga kugona moloza mapazi ake ku Qibla, kulavulira kapena kukodza ku Qibla, ndipo anthu ena ndikuyesa kumulangiza kuti asachite, ndipo wolangizidwayo ndi kunena kuti: ‘Ndikanakonda kuti tonse machimo athu akanakhala opweka chonchi,” ndikutheka kuti Iman ya oyankhulayo ingawononge ke. Pakuti wayankhula nga makruh ndi chinthu chosafunika pa malamulo.

Ngati wa ntchito wa munthu alowa m’chipinda cha bwana wake, bwanayo ali ndi munthu wina, napereka moni kwa bwana wake ponena kuti, “Salaam alaikum, bwana,” ndipo munthu wachitatu uja ndi kumukalipira wa ntchitoyo kuti: “Khala chete, munthu wakhalidwe loyipa iwe! Munthu sapereka moni kwa bwana wake motero.” Munthu wachitatuyo amakhala kafiri. Koma ngati cholinga chake ndi kuphunzitsa wa ntchitoyo malamulo a bwino ndipo amatanthauza kuti wa ntchitoyo akanatha kupanga malonjewo (mwakachetechete) mu mtima mwake, ndiye kuti kudzudzulako sikukhala kufuru.

Munthu akachita miseche ndipo ena ndikusonyeza kukhumudwa naye koma iye ndi kunena kuti “Sindinachite cholakwika kwambiri,” iye amakhala kafiri. Izi zili chonchi malinga ndi kunena kwa akatswiri a Chisilamu chifukwa iye wayamikira mchitidwe wa haram m’malo modzudzula.

Malinga ndi akatswiri a Chisilamu, kuyankhula kwa motere kufuru: “Allahu ta’âlâ atakandilowetsa ku Mparadiso, sindikalowa popanda iwe,” kapena “Enanu mukakalowa ku Mparadiso, Ine ndikanyanyalako” kapena “Ngati Allahu ta’âlâ atakandipatsa Mparadiso, ndidzakonda kuwona didar (nkhope yokongola) Yake." Mawu ena a ukafiri ndi kunena kuti iman idzachuluka kapena kuchepa. Malinga ndi Birgivi, ndi kufuru kunena kuti idzachuluka kapena kuchepa ponena za **mu’minun bih**, komae si kufuru ngati zikunenedwa

choncho ponena za yaqeen ndi quwwat-i-sidq. Poti ma mujtahid ambiri amayankhula za kuchuluka ndi kuchepa kwa iman.

Akatswiri a Chisilamu akuti ndi kufuru kunena kuti “pali ma Qibla awiri, Kaba ndi Yerusalemu.” Malinga ndi Birgivi, si kufuru kunena kuti, “Bayt-i-muqaddes inali Qibla Kaaba isanakhala Qibla.”

Munthu amakhala kafiri ngati adana kapena kutukwana katswiri ophunzira wa Chisilamu popanda chifukwa chomveka.

Ndi ukafiri kunena kapena kukhulupirira kuti zochita za chipembedzo ndi miyambo ya anthu osakhulupilira yosagwirizana ndi Chisilamu ndi zokoma.

Akatswiri ananena kuti munthu amene sakhuluppirira kuti kusalankhula pa kudya ndi mwambo umodzi wabwino kapena akati kugona ndi mkazi wako pomwe akudwala kumwezi kapena ku mchilo ndi khalidwe loyipa, amakhala kafiri.

Munthu akafunsidwa ngati iye ndi wokhulupilira ndipo winayo ndikuyankha: “Insha-Allahu,” koma ndikulephera kufotokoza, iye amakhala kafiri.

Akatswiri amanena kuti munthu akauza namfedwa kuti, “Mwana wako ndi wofunika kwa Allahu ta’âlâ,” iye amakhala kafiri.

Ngati mkazi wavala lamba wakuda m’chiwuno mwake ndipo atafunsidwa kuti ndi chiani iye ndi kunena kuti ndi zunnar (chovala chomwe anayenera kuvala omwe sanali Asilamu), iye amakhala kafiri ndipo amakhala haram kwa mwamuna wake.

Zanenedwanso kuti munthu wonena mawu oti, “Bismillah ...,” akudya chakudya chomwe chili cha haram amakhala kafiri. Hadrat Birgivi akunena kuti: “faqir yanena mwachimvekere kuti munthu ameneyo adzakhala kafiri ngati chakudyacho chiri haram li-’aynihi, mwachitsanzo vinyo, nyama yodetsedwa kapena mafuta a nyama imene yafa yokha. Koma, lamuloli limagwira ntchito ngati munthuyo akudziwa kuti chimene wadyacho ndi haram li-’aynihi, (chakudya choletsedwa m’Chisilamu). Potero adzakhala kuti wapeputsa Dzina la Allahu ta’âlâ. Pakuti zinthu za mtundu umenewu ndi za haram. Zafotokozeredwa ndi ma Imam athu (Atsogoleri achisilamu) kuti ngati munthu anena kuti, “Bismillah” pamene akudya chakudya chimene wapeza mwachinyengo, iye adzakhala kafiri ngakale kuti chakudyacho sichili choyipa pachokha. Koma chinyengocho ndi chomwe chiri

Haramu."[1] Koma akatswiri a chipembezo amalephera kugwirizana za munthu amene watembelera mnzake ponena kuti, "Allahu ta'âlâ adzachotse mzimu wako uli kafiri." Iwo sanagwirizane zoti ngati wonenayo amakhala kafiri.

Ndi kufuru munthu kuvomereze kuti iye ndi kafiri. Akatswiri ophunzira a Chisilamu amavomerezana izi. Ponena zovomereza kufuru kwa wina; malinga ndi akatswiri ena achisilamu amati ndi ukafiri pomwe akatswiri ena a kunena kuti ndi kufuru ngati chomwe chikuvomerezedwachi chili cha ukafiri. Koma si kufuru ngati chovomerezedwacho chili choipa ndi fisq (machimo) - kotero kuti chilango choperekedwa chikhale chamuyaya ndi chowopsa. Birgivi "rahima-hullâhu ta'âlâ" akuti: "Timamvetsa kuti qawl (chiweruzo cha ukadaulo) chimenechi ndi chofunika. Pakuti, nkhani yowona ya Hadrat Musa "alaihim-salâm"mu Qur'an al-Karim ndi umboni wake.

Ngati munthu atanena kuti: "Allahu ta'âlâ akudziwa kuti ine sindinachite zakuti zakuti," pomwe akudziwa kuti anazichita, iye amakhala kafiri. Pakuti ponena choncho wayika umbuli m'malo mwa nzeru kwa Hadrat Haqq ta'âlâ.

Ngati munthu akwatira mkazi pochita nikah popanda mboni ndikunena kuti mboni zawo ndi Allahu ta'âlâ ndi Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam", onse awiri amakhala makafiri. Chifukwa Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" sankadziwa ghayb (zobisika) pamene anali ndi moyo. Ndi kufuru kunena kuti akudziwa za Ghayb.

Munthu akanena kuti amadziwa za zinthu zobedwa ndi zotayika, iye komanso omamukhulupilira amakhala makafiri. Akanena kuti majini amamuuza, amakhalanso kafiri. Atumiki ndi majini sadziwa za Ghayb. Ndi Allahu ta'âlâ Yekha amadziwa za Ghayb, ndipo omwe amadziwa amawuzidwa ndi IYE.

Akatswiri a maphunziro akunena kuti ngati munthu akulumbilira mwa Allahu ta'âlâ koma wina n'kumukaniza kuti akufuna alumbire pa zinthu monga kusudzulana, kumasulidwa kwa kapolo, ulemu, ndi kudzisunga," wokana kulumbira kwa Allahu ta'âlâ yo amakhala kafiri.

Ndi kufuru kuwuza mnzake kuti, "Nkhope yako ikundikumbutsa za Mngelo wa Imfa." Pakuti, Mngelo wa Imfa ndi mngelo wamkulu.

Munthu amene amati "Sibwino kuchita namaz," amakhala kafiri. Akatswiri a Chisilamu amanenena kuti munthu akawuzidwa ndi

[1] Kuti mupewe kusamvetsetsana pankhaniyi, chonde werengani mutu woyamba wa fascicle ya chisanu ndi chimodzi ya **Endless Bliss**, yomwe ikupezeka kuchokera ku Hakikat Kitabevi, Fatih, Istanbul, Turkey.

mnzake kuti, “Bwerani mudzachite namaz,” ndipo woyitanidwayo ndi kuyankha kuti, “Ndizovuta kwa ine kuchita namaz,” woyitanidwayo amakhala kafiri.

Ngati munthu anena kuti, “Allahu ta’âlâ ndi mboni yanga kumwamba,” amakhala kafiri, chifukwa wayika malo kwa Allahu ta’âlâ. Allahu ta’âlâ ali wopanda malo. [Komanso, munthu kuyitana Allahu ta’âlâ kuti ‘bambo’ ndi kafiri.]

Ngati munthu atanena kuti, “Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” ankanyambita zala zake zodalitsika atatha kudya,” ndipo wina nkudzanena kuti ndi khalidwe loyipa limenelo, womalizayo amakhala kafiri.

Ngati munthu anena kuti: “Rizq (chakudya) limachokera kwa Allahu ta’âlâ, koma kutakataka kwa kapolo wobadwa ndi kofunika,” mawu akewo ndi osonyeza kupembedza milungu ina. Pakutinso kutakataka kwa munthu kumachitika ndi Allahu ta’âlâ. Ngati munthu anena kuti ndibwino kukhala Nasrani kusiyana ndi kukhala Myuda, (kapena kuti kukhala Mkafiri waku America kuli bwino kuposa kukhala Mkominisiti) amakhala kafiri. Kuli bwino munthu anene, mwachitsanzo, kuti Myuda ndi woyipa kuposa Nasrani kapena kuti Mkominisiti ndi woipa kwambiri kuposa Mkhristu.

Ngati munthu atanena kuti kukhala kafiri ndi kwabwino kuposa kuchita chinyengo, amakhala kafiri.

Munthu akanena kuti alibe nazo ntchito za ilm (kuzindikira) kapena “Ndikovuta kuchita zomwe Maulama akunena,” kapena iye kutaya ma fatwa (olembedwa) kapena kunena kuti “Mawu a anthu opembedza si abwino,” iye amakhala kafiri.

Anthu akakangana ndipo mmodzi ndi kumuuza mnzakeyo kuti, “Tiyeni tikasume ku Shar’ (khoti la Chisilamu),” ndipo wowuzidwayo ndi kuyankha kuti, “Sindipita kumeneko pokhapokha apolisi adzanditenge,” kapena “Zindikhudza bwanji za Chisilamu,” womalizayo amakhala kafiri.

Ngati munthu anena chinthu choyambitsa kufuru, iye komanso amene asekenawo amakhala makafiri. Kuseka kwa enawo sikudzakhala kufuru ngati kuli daruri (kosapeweka, kongochitika, kosatheka kupilira).

Munthu yemwe akunena kuti, “Palibe malo [opanda kanthu] posakhala Allahu ta’âlâ,” kapena “Allahu ta’âlâ ali kumwamba,” amakhala kafiri, malinga ndi akatswiri ophunzira a Chisilamu.

Munthu amene amanena kuti mizimu ya meshaikh (anthu oyera) imakhalapo nthawi zonse ndipo akudziwa, amakhala kafiri. Sikudzakhala kufuru kunena kuti iwo adzakhalapo.

Munthu akanena kuti, "Sindikudziwa (kapena sindikufuna) Chisilamu," amakhala kafiri.

Munthu wonena kuti, "Adam "alaihim-salâm"akanapanda kudya chipatso, sitikadakhala ma shaqi (otchimwa, ochita zoipa)," amakhala kafiri. Komabe pali kusiyana pakati pa akatswiri ophunzira a Chisilamu ngati chimangirizocho chitathera kuti, "...bwenzi tisali padziko pano".

Ngati munthu anena kuti 'Adam "alaihim-salâm" ankaluka nsalu ndipo wina nkudzanena kuti, "Ndiye kuti ndife ana a mmisiri oluka nsalu," womalizayo amakhala kafiri.

Munthu akachita tchimo laling'ono ndi kuwuzidwa kuti achite tawba, iye ndikufunsa kuti: "Kodi ndachita tchimo lanji kuti ndichite tawba," amakhala kafiri.

Munthu akamuwuza mnzake kuti, "Tiyeni kwa katswiri wa maphunziro a Chisilamu," kapena "Tiye tiwerenge mabuku a Fiqh ndi Ilm-i-hal kuti tiphunzire," ndipo wowuzidwayo ndi kuti, "Kodi ilm ndi ya ntchito yanji kwa ine?" wofunsayo amakhala kafiri. Chifukwa potero wanyoza 'ilm. Munthu amene amanyoza, kapena kunyozetsa mabuku a Tafsir kapena Fiqh, amakhala kafiri. Makafiri osatheka omwe amatsutsa mabuku ofunika olembedwa ndi akatswiri a Madhhab anayiwa, amatchedwa 'a Science a matsenga' kapena "zindiqs".

Munthu amene sadziwa mayankho a mafunso monga, "Ndinu ana a m'bado wandani?", "Ndinu a millat yanji?", "Kodi Imam wa Madhhab anu mu i'tiqad ndi ndani? ndi "Imam wa Madhhab anu mu amal (zochita za chipembezo) nid ndani?", amakhala kafiri.

Akatswiri ophunzira a Chisilamu akuti munthu yemwe akuti "Halal," akunena chinthu cha haram-i-qat'iyya –monga vinyo ndi nyama ya nkhumba, kapena kunena "haram," zinthu za halali-qat'iyya (zinthu zomwe ndi halal), amakhala kafiri. [Ndi zowopsa kunena kuti fodya ndi haram.]

Ndi kufuru kufuna kuti mchitidwe wa haram ukanakhala wa halal pomwe mchitidwewo ndi wa haram (oletsedwa) m'zipembedzo zonse. Ndipo zingakhale zotsutsana ndi hikmat (nzeru) kuchichita chinthucho kukhala halal. Zitsanzo za izi ndi dama, chiwerewere, kudya utakhuta, ndi kutenga kapena kupereka chiwongola dzanja. Si kufuru kukhumba kuti vinyo akhale halal pakuti vinyo sanali haram m'nthawi zonse (zakale). Ndi kufuru kugwiritsa ntchito Qur'an al-kareem pakati pa

mawu ndi nthabwala. Ngati munthu amunena mnzake yemwe dzina lake ndi Yahya, "**Ya Yahya! Huz-il-kitaba**," amakhala kafiri chifukwa wachitira chipongwe Qur'an al-kareem. Lamulo lomweli likugwiranso ntchito powerenga Qur'an al-kareem pomwe zida zoyimbira zikuyimbidwa kapena pakati pa magule kapena nyimbo. Ndi afat[1] kunena kuti, "Ndangofika kumene, Bismillahi." Ngati munthu akuti "**Ma khalaqallahu,**" akaona chinthu chimene amachiona kwambiri, amakhala kafiri ngati sakudziwa tanthauzo lake.

Ndi afat kunena kuti, "Sindikutukwana tsopano, pakuti kutukwana ndi 'tchimo'.

Ndi afat kunena kuti, "Mwakhala maliseche ngati mwana wa ng'ombe ya Jabraili." Kuteroko ndikumuseka Mngelo Wamkulu.

Ndi haram kulumbira potchula chinthu china osati Allahu ta'âlâ. Munthu sangakhale murtadd (wopatuka) kapena kafiri pochita za haram. Koma adzakhala kafiri ngati anena halal pa chinthu cha haram zomwe zili mansusun alaih, (zomwe zanenedwa kuti ndi haram mu Nass, yomwenso imatanthauza ayat-i-karimas ndi hadith-i-sharifs momveka bwino).

Ndipo kulumbira kwa mtundu uwu kukhonza kukhala kufuru: "Wallahu ndikulumbira pa mutu wa mwana wanga kapena wallahu ndikulumbira khate.

AHKAM AL-ISLAMIYYA

M'chipembedzo cha Chisilamu zolamulidwa ndi zoletsedwa zonse pamodzi zimatchedwa **Ahkam Al-islamiyya** kapena **Chisilamu**. Ahkam Al-islamiyya ndiyopangidwa ndi zigawo zisanu ndi zitatu zomwe ndi: **fardh**, **wajib, sunnah, mustahab, mubah, haram, makruh, ndi mufsid.**

Fardh ndi lamulo la Allahu ta'âlâ. Popeza ndi lamulo Lake, lafotokozedwa momveka bwino ndi ma umboni otsimikizirika m'ma ayat-i-karima. Munthu wokanira kapena wosalemekeza lamulo lotero amakhala kafiri. Zitsanzo za malamulo a Allahu ta'âlâ omwe amatchedwa fardh ndi: Iman, Qur'an, udhu, kuchita namaz, kupereka zakat, kuchita Haji, kusamba mukatha junub, (kusamba thupi lonse m'njira yophunzitsidwa ndi Chisilamu.)

Pali ma fardh amitundu itatu: fardh-i-daim, fardh-i-muwaqqat, ndi fardh-i-ala-l-kifaya. Fardh-i-daim ndiko kuloweza nsanamira zisanu ndi

[1] Afat ndi mawu ochuluka a afet, omwe tanthauzo lake la lexical ndi tsoka, tsoka, chiwonongeko.

imodzi za Chikhulupiliro zomwe zimayamba ndi: **Amantu billahi ...** Kuzindikira ndi kukhulupilira matanthauzo ake, ndi kuzisunga nthawi zonse. Fardh-i-muwaqqat ndi kupembeza kulikonzse kolamulidwe komwe timachita nthawi yake ikakwana. Zitsanzo zake ndikuchita namaz kasanu pa tsiku, kusala chakudya (kufunga) m'mwezi wodalitsika wa Ramadan, ndi kuphunzira luso la nthambi ya zaluso kapena za malonda. Fardh-i-'ala-l-kifaya ndi lamulo la Allahu lomwe akachita munthu mmodzi, malipiro ake amapita ku gulu lonse la anthu, kaya alipo makumi asanu, zana, ndi ena otero. Chitsanzo chake ndi kuvomera salaamu.

Zitsanzo zina ndi monga kuchita namaz ya janaza, kusambitsa mtembo wa Msilamu akamwalira, kuphunzira malamulo a chiyankhulo cha Chiarabu otchedwa sarf ndi nahw, kukhala hafiza, kuphunzira nthambi ya chidziwitso yotchedwa wujub, ndi kuphunzira za chipembedzo ndi sayansi ya chidziwitso modzama.

Palinso ma fardh ena asanu mkati mwa fardh. Ma fardh amenewa ndi: Ilm-i-fardh, amal-i-fardh, miqdar-i-fardh, i'tiqad-i-fardh, ikhlas-i-fardh, ndi inkar-i-fardh. Inkar-i-fardh ndi kufuru.

Wajib ndi lamulo la Allahu ta'âlâ lomwe umboni wake siunasimikizike kapena kummveka bwino. Munthu akakana chinthu chomwe chanenedwa kuti ndi wajib sadzakhala kafiri. Koma kusachita ntchito za wajib kukamuyika munthu m'mazunzo ku Jahannama. Zitsanzo zake ndi izi: Kuchita Qunut pa nthawi ya Namaz ya Witr, kuchita Qurban, (kupha nyama yotchedwa qurban m'njira yovomerezeka) mu nthawi ya Eid Aduh, kupereka chopereka chotchedwa Fitra mu nthawi ya Eid pakutha pa mwezi wa Ramadan, ndi kuchita sajda yotchedwa **Sajda-i-tilawat** pomwe mukuwerenga kapena kumva ayah ya sajda (kugwadira). Pali ma wajib ena anayi ndi fardh imodzi mkati mwa wajib: Ilm-i-wajib, amal-i-wajib, miqdar-i-wajib, i'tiqad-i-wajib, ndi ikhlas-i-fardh. Ndi haram kudzionetsera pochita ntchito ya fardh kapena wajib.

Sunnah ndi ntchito yopembedza yomwe Hadrat Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anasiya kuchita kamodzi kapena kawiri basi. Munthu sakazunzidwa pa tsiku lomalizachifukwa chosachita Sunnah. Koma ngati munthu ali ndi chizoloŵezi chosiya Sunnah popanda udhr (chifukwa chomveka) chosiyira, adzalandira itab (chitonzo) pa tsiku lomaliza. Komanso sadzapeza kapena kulandira thawab za Sunnah. Zitsanzo za Sunnah ndi izi: Kugwiritsa ntchito miswak potsuka mano, kuchita azan ndi iqamah, kuchita namaz pa jama'at, kudyetsa anthu madzulo a tsiku la ukwati wako, ndi kuchita

mdulidwe mwana kapena ana ako amuna. Pali mitundu itatu ya Sunnah: Sunnah-i-muakkada, Sunnah-i-ghayr-i-muakkada, ndi Sunnah-i'ala-l-kifaya.

Zitsanzo za Sunnah-i-muakkada ndi izi:

Sunnah musanachite namaz ya m'mawa (fajir), Sunah musanachite komanso mutatha namazi ya masana (Dhuhr), Sunnah mutatha namaz yamadzulo (Magrib), ndi Sunnah mutatha swala ya usiku (Eisha). Sunnah izi ndi Sunnah-i-muakkada. Akatswiri ena ophunzira a Chisilamu amati Sunnah yopemphera m'mawa ndi wajib. Ma Sunnah awa sangasiyidwe popanda udhr. Munthu wonyoza iliyonse mwa izi amakhala kafiri.

Zitsanzo za Sunnah-i-ghayr-i-muakkada ndi izi: Sunnah musanachite namaz ya masana (Asr) ndi Sunnah musanachite namaz ya usiku (Eisha). Kusachita ma sunna kulibe chilanga koma kungam'nyozetse munthu ndi kumutsekereza shafa'at (uwomboli wa tsiku lomaliza).

[Zalembedwa mu **Halabi** ndi mu **Quduri**, kuti pali magulu awiri a mapemphero: **Fardh** ndi **Fadail**. Ntchito zopembedza zomwe si fardh kapena wajib zimatchedwa fadail kapena nafila (zoyenjezera). Ma Sunnah a mapemphero asanu a pa tsiku ali m'gulu la kulambira kwa nafila, ndipo amazazitsira mzofooka za m'ma fardh. Ma Sunnah amenewa amabwezera zolakwika m'machitidwe a fardh mbali za mapemphero. Mumvetsetse izi. Pemphero la Sunnah silingalowe mmalo mwa pemphero la fardh lomwe siminachite, ayi. Ndipo ndipo munthu sangakapulumuke ku chilango chosachita namaz ya fardh chifukwa waswali Sunnah. Swalah ya Sunnah yopempheredwa ndi munthu amene wasiya Swalah ya fardh popanda 'udhr siidzakhala sahih. Niyyah (chitsimikizo) n'chofunika pa pemphero la Sunnah lomwe ndi sahih (yovomerezeka).

Ngati niyyah siipangidwa, thawab za Swalah ya Sunnahyo sizingapezeke. Choncho, anthu amene sanapemphere Swalah zawo za pa tsiku kwa zaka zambiri, ayenera kupanga niyyah yawo yochita qadha ya Swalah zoyandikira zomwe sadachite. Achitenso Sunnah monga momwe amachitira ma Sunnah anayi a Swalah za pa tsiku. Akapanga niyyah motero ndiye kuti adzakhala atapanga qadha ya magawo a fardh a ngongole zawo za Namaz ndikuchita mbali za Sunnah za zomwe zilipo pa nthawiyo. Kuchita zimenezi sikukutanthauza kusiya Sunnah.]

Sunnah-i-'ala-l-kifaya ndi mtundu wa Sunnah womwe gulu lonse lokhudzidwa lidzakhululukidwa ngati yachitidwa ngakhale ndi munthu

m'modzi wa gululo. Zina mwa zitsanzo ndi: Kupereka malonje, kuchita m'bindikiro wotchedwa i'tikaf, ndi kunena kuti: "Bismillah-ir-Rahman-ir-Rahim," poyamba kuchita chinthu chololedwa ndi Chisilamu.

Munthu akapanda kunena Bismillah pamene akuyamba kudya, adzaluza zinthu zitatu: 1- Satana adzadya naye chakudyacho. 2– Chakudyacho chidzasanduka matenda m'thupi mwake. 3- Muchakudya chimene wadya simudzakhala Baraka (madalitso).

Akanena Bismillah, chakudya chomwe akudya chidzapereka pindu motere: 1- Satana sapeza gawo la cha kudyacho. 2-Chakudya chomwe wadya chimakhala chochiritsa mthupi mwake. 3- Muzakudya mudzakhala baraka. [Ngati munthu wayiwala kunena Bismillah pamene akuyamba kudya, anena pamene wakumbukira.]

Mustahab ndi chinthu chimene Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anachita kamodzi kapena kawiri m'moyo wake wonse. Munthu amene sachiata ntchito za mustahab sadzazunzidwa kapena kunyozedwa pa tsiku lomaliza. Ndiponso sadzamanidwa shafa'at (uwomboli wa tsiku lomaliza) chifukwa chosachita mustahab. Zitsanzo mustahab ndi: Kuchita nafila namaz (namazi yapadera), kusala kapena kufunga kwapadera, kuchita Umra, kuchita Haji yapadera, ndi kupereka sadaka mochulukitsa.

Mubah ndi ntchito (yololedwa) yomwe umalipidwa nayo ndi thawab ikachitidwa mchifuniro chabwino ndipo imadzetsa chilango pa tsiku lomaliza ikachitidwa ndi mchifunira choyipa. Kupanda kuchita sikudzetsa vuto lirilonse. Zitsanzo zina ndi izi: Kuyenda, kukhala, kugula nyumba, kudya zakudya za mtundu uliwonse zomwe ziri halal, komanso kuvala zovala za mtundu uliwonse, malinga ngati zili za halal.

Haram ndi chinthu chomwe Allahu ta'âlâ akuletsa momveka bwino mu Qur'an al-kareem. Mwachidule ndi chimodzi mwa 'zoletsedwa kuzichita' zofotokodwa mu Qur'an al-kareem. Munthu amene wayitenga haramu mopepuka kapena kuyikana, amakhala kafiri. Munthu amene wachita haramu akudziwa kuti ndi haramu, sakhala kafiri. Iye amakhala fasiq (wampwanya malamulo). [Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ" akunena motere pa nkhani yokhudzana ndi kukhala imam:[1]

"Musachite namaz ya jamaah yotsogoleredwa ndi imam wa fasiq. Fasiq ndi Msilamu ochita tchimo lalikulu monga kumwa mowa, dama, ndi kutenga chiwongola dzanja. [Tchimo lochepa lomwe limachitika mosalekeza limakula kwambiri kukhala tchimo lalikulu.] Kumadera

[1] Imam, mu nkhaniyi, ndi Msilamu amene amatsogolera Namaz ya jama'at.

komwe pemphero la Lachisanu likuchitika m'mizikiti yoposa umodzi, pempherani Swalah ya Jummah mu mzikiti womwe pali Imam wa Salih osati yemwe ndi fasiq. Ndi wajib kunyoza ndikuchitira chipongwe munthu wa fasiq. Ngakhale munthu atakhala wophunzitsidwa bwino, sayenera kupangidwa kukhala imam.

Ndi wajib kumukanira ndi kusiya kumulemekeza munthu yemwe ndi fasiq. Munthu yemwe ndi fasiq asakhale imam ngakhale ataphunzira kwambiri. Kumupanga imam kudzatanthauza kuti iye ndi munthu wa ulemelero komanso wolemekezeka. Ndi makruh tahrimi kumupanga fasiq yemwe satsatira imodzi mwa Madhhab anayi aja, kukhala imam. Kupewa za haram kumatchedwa **taqwa**. Ndi **wara** (umulungu) kupewa zinthu zomwe ziri zokayikitsa kuti ndi halal kapena haram. **Zuhd** ndi kuzisunga; kusagwiritsa za halal kuopera kuti ungachite chinthu chokayikitsa. Ngati munthu yemwe akhala akukhala ku Dar-ul-harb akulowa Chisilamu, zili wajib kwa iye kusamuka kupita ku Dar-ul-islam."]

Pali mitundu iwiri ya haram: **haram li-'aynihi** ndi **haram li-ghayrihi**. Haram li-'aynihi ndi haram yomwe ili yokhazikika mwa iyo yokha; ndipo imakhala haram nthawi zonse. Zitsanzo ndi: Kuphana, dama, chiwerewere, kumwa mowa kapena zakumwa zina zoledzeretsa, njuga, kudya nyama ya nkhumba, ndi kutuluka kwa akazi ndi atsikana m'nyumba ndi kumayenda mitu yawo, mikono ndi miyendo yawo ili pamtunda. Ngati munthu anena Bismillah pochita machimo omwe tatchulawa, amakhala kafiri. Munthu akakhulupilira kuti machimo omwe tatchulawa ndi Halal, kapena kuti sakuona kufunika komwe Allahu ta'âlâ anachitira zinthu izi kukhala haram, ameneyonso amakhala kafiri. Koma ngati anthu achita machimo amenewa akukhulupilira kuti ndi za haram, kotero kuti amaopa chilango chimene Allahu ta'âlâ adzawatsitsire, iwo sadzakhala makafiri, koma adzayenera kulandira chilango kumoto.

Haram li-ghayrihi ndi chinthu chomwe sichili haram kwenikweni koma kuti chapezeka m'njira ya haram. Mwachitsanzo, kulowa m'munda wa zipatso wa mwini popanda chilolezo ndi kuthyola zipatso ndi kudya, kuba katundu kapena ndalama za mwini ndi kuziwononga. Ngati munthu akunena Bisimillah pochita izi kapena kunena kuti ndi halal kuchitia izi, iye sadzakhala kafiri. Munthu akatenga mwa chinyengo chuma cha wina cholemera ngati kanjere ka chitowe m' dziko lino la pansi, Allahu ta'âlâ adzalanda munthu ameneyo thawab za ma rakat mazana asanu ndi awiri (700) a namaz zochita pa jama'ah ndipo zomwe zinalandilidwa ndi Allahu ta'âlâ. Pali thawab zochuluka

zedi popewa kuchita zinthu za haram za mtundu uliwonse kuposa kuchita mapemphero.

Makruh ndi zinthu zomwe zimaononga thawab zopezedwa mu njira ya amal (ntchito zopembedza, kulambira ndi kuchita zabwino). Pali mitundu iwiri ya makruh: Karahat-i-tahrimiyya ndi karahat-i-tanzihiyya. Ena amati: makruh tahrimi ndi makruh tanzihi.

Makruh tahrimi (Karahat-i-tahrimiyya) ndi kusiya chinthu chomwe ndi wajib. Makruh tahrimi ndi qarib (ndi yoyandikira) ku haram. Ngati munthu wachita makruh tahrimi, amakhala wosamvera ndi wochimwa ngati wachita mwadala. Ndipo ayenera kukalowa ku moto wa Jahannama. Ngati wachita izi pa nthawi ya Namaz, adzayenera kuyichitanso Namaziyo. Ngati wachita mwa sahw (molakwitsa, moyiwala) adzayenera kuchita sajda-i-sahw (pamapeto a Namaz). Ndipo sikudzafunika kuchitanso Namazyo. Makruh tanzihi (Karahat-i-tanzihiyya) ndi kusiya chinthu chomwe ndi Sunnah. Ndi qarib ku halal. Munthu amene wachita chinthu chomwe ndi makruh tanzihi sangalandire chilango patsiku lomaliza. Koma ngati achita mwa chizolowezi, akuyenera kutonzedwa ndi kulandidwa shafa'at[1] pa tsiku lomaliza. Zitsanzo za izi ndi: Kudya nyama ya hatchi, kudya zotsalira za chakudya chodyedwa ndi mphaka kapena mbewa, ndi kugulitsa mphesa kwa wopanga vinyo.

Mufsid ndi chinthu chomwe chimaononga etsa amals (ntchito zopembedza ndi ntchito zina zabwino). Zitsanzo za ntchito zambwino zomwe zingaononga eke ndi: Kuononga iman, namaz, nikah, hajj kapena zakat zochitika, komanso kugula ndi kugulitsa komwe kukuchitika.

[Msilamu amene amachita zinthu za fardh, wajib, ndi Sunnah ndipo amapewa kuchita zinthu za haram ndi makruh adzalandira **ajr** (malipiro) kapena kuti **thawab,** pa tsiku lomaliza. Ngati munthu akuchita za Haramu ndi makruh koma osalabadira fardh ndi wajib, adzalembedwa ngati munthu **wochimwa**. Thawab zopeza pa kupewa haramu ndi zochuluka kuposa thawab zopeza pochita fardh. Thawab zopeza pochita fardh ndi zochuluka kuposa thawab zopeza popewa makruh, zomwe zimakhala zochulukirapo kuposa thawab za Sunnah. **Khayrat** ndi **Hasanah** (zachifundo ndi ntchito za chipembedzo) ndi ma mubah (zinthu ndi ntchito zololedwa) ena omwe Allahu ta'âlâ amakonda. Ngakhale kuti thawab zidzaperekedwa kwa munthu

[1] Kuchonderera kwa Allah kudzera mwa bwenzi la pa mtima la Allah kuti akhululukidwe wochimwa wokhulupirira

amene wazichita zimenezi, thawab zimenezo ndi zocheperapo tikafanizira ndi thawab zochita ntchito ya Sunnah.

Qurbat ndi kuchita chinthu mozindikira kuti munthu udzapatsidwa malipirhitao pa chomwe ukuchicho.

Allahu ta'âlâ mwini chisoni kwambiri ndi akapolo Ake, anawatumizira zipembedzo zomwe ndi magwero la chitonthozo ndi chisangalalo. Chipembedzo chomaliza ndi chipembedzo cha nthawi ya Muhammad "alaihim-salâm". Zipembedzo zina zinasinthidwa ndi anthu oyipa. Munthu aliyense, kaya Msilamu kapena si Msilamu, akukhala moyo wotsatira chipembedzochi, kaya iye akudziwa potsatirapo kapena sakudziwa, munthu ameneyo sadzapeza mavuto pa dziko la pansi.

Chitsanzo pa mfundo imeneyi ndi anthu osakhulupilira a ku Europe ndi ku America amene akugwira ntchito yogwirizana ndi chipembedzochi. Koma anthu osakhulupilira sadzapatsidwa thawab kapena malipiro aliwonse pa tsiku lomaliza. Koma ngati munthu yemwe akugwira ntchito yonga iyi ali Msilamu ndipo akufuna kumvera chiphunzitso cha Chisilamu, iyeyo pa tsiku lomaliza adzapeza chisangalalo chosatha.]

NSICHI ZA CHISILAMU

Chisilamu chiri ndi nsichi zisanu, kapena kuti Chisilamu chamangidwa pa zinthu zisanu zofunika. Nsichi yoyamba ndi kunena Kalima-i-shahadat, ndi kuyiphunzira komanso ndi kukhulupilira tanthauzo la Kalima-i-shahadat. Yachiwiri ndi kuima ndi kupemphera (Namaz), Swalah zisanu pa tsiku mu nthawi yake yoyikidwa. Nsichi yachitatu ndi kusala kudya (kufunga) tsiku lirilonse m'mwezi wodalitsika wa Ramadhan. Nsichi ya chinayi ndi kupereka zakat ndi 'ushr chaka chirichonse, panthawi yoti ndi fardh kutero. Nsichi yomaliza ndi kupita ku Haji kamodzi pa moyo wa munthu, ngati kuli kothekera kutero kwa iye. [Kuchita malamulo asanu awa a Allahu ta'âlâ, pamodzi ndi kupewa zoletsa zake (haram), kumatchedwa **kupembedza**. Koma kupita ku Haji si kokakamizadwa kwa Msilamu yemwe sangakwanitsa zofunikira kukhala nazo kuti munthu apite ku Haji. Zofunika izi zimatchedwa wujub ndi ada. Kwa munthu wotere Haji imakhala nafila. Chimodzimodzi kwa munthu yemwe wapita kale ku Haji, Haji imakhala Nafila kwa iye ngati atachitenso. Si jaiz (zololedwa) kuchita ntchito za chopembedza zomwe zili Nafile ngati kutero kungapangitse kuchita bidah kapena haram. Hadrat Imam Rabbani

quddisa sirruh, m'ma kalata ake a makumi awiri ndi mphambu zisanu ndi zinayi (29), zana ndi makumi awiri ndimphambu zitatu (123) ndi kalata ya zana limodzi ndi makumi awiri ndi anayi (124), Komanso Abdullah Dahlawi 'quddisa sirruh', mu kalata yake ya makumi awiri ndi mpambu zisanu ndi chimodzi (26) ya **Maqamat-i-Mazhariyya**, musapereke chilolezo cha Hajj ya nafila kapena Umra. (Afif-ud-din Abdullah bin As'ad Yafii "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" , 698 [1298 A.D.], Yemen – 768 [1367], Makka, akunena motere mukuunika kwake pa za 'zuhd' (kudziletsa ndi kufuna chisangalalo cha Allah) yomwe ndi sitepe ya maqamat-i-ashara [ya khumi (10)], m'bukhu lake lotchedwa **Nashr-ul-mahâsin-il-ghâliyya**:

Imam Nawawi, mmodzi mwa akatswiri akulu a Chisilamu komanso wali anafunsidwa kuti: 'chifukwa chani mumatsatira ma Sunnah onse kupatula Sunnah imodzi yomwenso ili Sunnah yofunikira yomwe ndi nikkah?' Iye anayankha 'ndikuopa kuchita ntchito zambiri za haram pomwe ndikupanga ntchito ya Sunnah imodzi." Imam Yahya Nawawi anamwalira ku Damascus mchaka cha 676 [1277 A.D.]. Prof. Habib-ur-Rahmin, mkulu wa Jami'ai-habibiyya yaku Pâkistân, anapita ku Haji mu 1401 [1981 A.D.]. Ataona kuti Imam wa Wahhabi akutsogolera namaz ya jamaat pogwiritsa ntchito chimkweza mau, Iye anachita namaz yake payekha. Pakutero anamangidwa ndikuponyedwa mndende. Atafunsidwa kuti ndi chifukwa chani sanapemphere pa jamaah, iye ananena kuti si kololedwa imam kutsogolera mapemphera a gulu pogwiritsa ntchito chimkwezamau. Anayimitsidwa kuti asapange Haji ndipo anatulutsidwa mdzikolo.

Munthu ukapita kwina kulikonzse, chinthu chofunika choyamba ndi kuphunzira chikhulupiriro ndi iman yakho. Kale kunali kosavuta kuphunzira chiipembezo kuchokera kwa akatswiri a chisilamu. Koma makono kulibe akatswiri a chisilamu omwe atsala. Mbuli ndi zitsiru za anthu zogudwa ndi azungu aku Britain aupandu afalikira ponseponse m'dzina la anthu chipembezo. Njira yatsala yophunzirira chikhulupiriro ndi iman ndi kuwerenga mabuku olembedwa ndi akatswiri a Ahl as-Sunnat. Kupeza mabukhu amenewa ndi chisomo cha Allah ta'âlâ. Adani a Chisilamu akufalitsa mabuku abodza a chipembezo ndi cholinga chosokoneza achinyamata. Chocho ndikovuta kupeza mabuku achipembezo enieni. Achinyamata sakukhazikika. Atanganidwa ndi kusangalatsidwa ndi masewera osiyanasiyana opusa ndipo potero alibe nthawi yopeza ndi kuwerenga mabuku owona. Ndi zomvetsa chisoni kuti pali umboni wokwanira wakuti achinyamata ambiri samalingalira kalikonse koma masewera. Nthenda imeneyi

ikufalikira mwa achinyamata. Ndikofunikira kwambiri kuti makolo a Chisilamu ateteze ana awo ku mliri umenewu. Izi achite podziwitsa ana awo za chikhulupiliro chawo ndi kuwazoloweza kuwerenga mabuku a chipembedzo.

Ateteze ana kuti asakonde kutaya nthawi yawo pa zinthu zowononga. Timaon ana a anzahu amene tikuwadziwa atatanganidwa kwambiri ndi masewera oipa moti mpaka amayiwala kudya chakudya chawo. Ndikovuta ana otere ngakhale kuti awerenge mabuku akusukulu ndi kukhonza mayeso. Makolo ayenera kulimbikitsa ana awo kuwerenga mabuku. Mwachitsanzo awerenge bukhu la 'Makhalidwe a Chisilamu'. Munthu akawerenge bukhu limeneli, adzaphunzira chikhulupiriro chake ndi iman. Komanso azadzama ndikudziwa zobisika za adani a chisilamu ndi momwe amaganizira. Ngati makolo anyalanyaza udindo wawo, dziko lathu lizadzadza ndi achinyamata osapembedza ndi osakhulupilira omwe adzawononge dzikoli.

Nkhani ina imene makolo ayenera kuyikirapo mtima kwambiri ndiyo nkhani ya 'satr-i-awrat' (ziwalo zobisika) yomwe yalongosoledwa mwatsatanetsatane pa mutu wachisanu ndi chitatu (8) gawo lachinayi m'buku la **Endless Bliss**. Tikuona achinyamata ziwalo zili panja kuyambira mmaondo mpaka mmichombo pakati pa anthu akusewera masewera oipa. Ndi ntchito yofunikira ndipo ndi fardh kuphimba ziwalo zobisika. Anthu omwe sawona kufunika kwa izi akhoza kutaya iman. Asilamu amapita ku mizikiti ndi cholinga chofuna kupeza thawab zochuluka pochita Namaz. Komanso kukamvera ulaliki. Ngakhala popanda izi, kupita ku mzikiti kumapereka thawab zambiri. Kumalo komwe anthu amacheza ziwalo zobisika zikuowonekera poyera sangakhale mzikiti; malo otero ndi pokumanirana ma fisq (ochimwa). Kwalembedwa m'mabuku onse (a Chisilamu) kuti ndi haram kupita komwe amakumana ma fisq. Anthu amene angapite ku mizikiti atavala motero adzakhala ngati apita ku misonkhano ya fisq; adzakhala ochimwa. Munthu amene amapita ku mizikiti asanavale bwino ndi cholinga chofuna kukapeza thawab ndi kumvera ulaliki wa chipembedzo amapeza machimo mmalo mopeza thawab. M'mizikiti mukalowa anthu owonetsa ziwalo amawachititsa Asilamu kukhala ochimwa. Ndi tchimo lalikulu kuonetsa mbali za awrat (pakati pa anthu ena). Ndi tchimonso lalikulu kuyang'ana ziwalo za ena za awrat. Choncho, Asilamu amene amapita ku Mizikiti atavala mosalongosoka amakapeza utchimo ndipo potero amabweretsa Ghadab-i-ilahi (Mkwiyo wa Allahu ta'âlâ) mmalo mopeza thawab.]

NAMAZ (SWALA)

Namaz ili ndi ma farza (magawo) khumi ndi awiri (12): asanu ndi awiri (7) a iwo ali kunja kwake, ndipo asanu (5) ali mkati mwake. Ma farza amene ali kunja kwa Namaz ndi: Taharat (kudziyeretsa, ukhondo) kuchokera ku hadath; taharat kuchokera ku najasat; satr-i-awrat (kudziphimba); istiqbal-i-qibla (mbali yoyang'ana); waqt (nthawi yokhazikitsidwa); niyyah (cholinga); takbir-i-iftitah. Ma farza a m'kati mwake namaz ndi: Qiyam (kuyima kuyamba swala); qiraat (Kusoma); ruku (kuwerama pa swala) kamodzi pa rak'at iliyonse; sajda (kugwetsa nkhope pansi pa swala) kawiri mu rak'at iliyonse; kukhala nthawi yayitali kunena tashahhud pa qa'da-i-akhira komwe ndi kukhala komaliza. Ma farza a m'kati mwa Namaz amatchedwa ma **rukn**. Ndi fardh kugunditsa chiphumi ndi zala zazikulu zakumiyendo pansi pa nthawi ya sajda.

Taharat ya hadath ndi kuchita udhu ngati munthu alibe udhu, kuchita ghusl (kusamba) ngati ali ndi janaba; ndi kuchita tayammamu (kugwiritsa ntchito dothi) ngati kulibe madzi pamene munthu akufunika udhu kapena kuchita ghusl. Zinthu zitatu zitsatidwe kuti taharat ya hadath ikwaniritsidwe:

Kutsatira bwino lomwesunga za istinja ndi istibra, (zomwe zidzafotokozedwa mtsogolomuno) posamba ndi pochita masah pa mutu. Osasiya malo aliwonse omwe ali fardh osasambitsidwa.

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti taharat ya najasat ikwaniritsidwa: Kuyeretsa zovala zomwe zivalidwe pochita namaz kuchokera ku najasat. Kuyeretsa thupi lako pochita namaz. Kuyeretsa malo ochitira namaz. [Chonde onani kumapeto kwa mutu womwe ukunena za magawo makumi asanu ndi anayi (54) a ma Farze!]

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti satr-i-awrat ikwaniritsidwe: Mu Madhhab a Hanafi, amuna ayenera kuvala kuchokera pa mchombo pawo mpaka pansi pa mawondo awo. Ndi Sunnah kwa amuna kuphimba mapazi awo pochita Namaz.

Kwa akazi a ufulu ayenera kuphimba thupi lawo lonse kupatula nkhope zawo ndi manja awo. Malinga ndi lipoti la akatswiri (riwayat), mapazi awo ata kuonetsakera.

Kwa akazi omwe ali m'gulu lotchedwa ma jariya ayenera kuphimba tupi lawo kuyambira kumtunda kwa misana ndi mabere mpaka pansi pa mawondo awo. [Akazi omwe amayenda, mitu, mikono ndi miyendo yawo ili pamtunda kapena kuvala zovala zothina ndi zopyapyala ndi amuna omwe amayang'ana izi, onse ndi ochimwa chifukwa chochita

haramu pakutero. Munthu amena akuchitira ugonthi izi posawona kuti ndi haram amakhala kafiri, murtadd.]

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti istiqbal-i-qibla ikwaniritsidwe: Kutembenukira ku Qibla. Osalola kuti chifuwa chako chitembenuke kuchoka ku Qibla mpaka Namaz itatha. Kudzichepetsa mu diwan-i-ma'nawi (pozilembetsa mkaundula) wa Allahu adhîm-ush-shân.

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti waqt (nthawi ya namaz) ikwaniritsidwe: Kudziwa nthawi yomwe Namaz ikuyambira ndi nthawi yomwe ikuthera. Kusachedwetsa Namaz mpaka kulowa mu nthawi yomwe ili makruh. Kuchita niyyah mozindikira ndipo mo kukhazikika mu mtima mwanu potchula namaz yomwe mukuyenera kuchita kaya ndi fardh, wajib, Sunnah kapena mustahab. Iwalani zokonda zanu za mdziko mu mtima mwanu.

Kupemphera namaz ya Witr ndi wajib malinga ndi Imam A'zam. Koma ndi Sunnah malinga ndi ma imam awiri a Imameyn, omwe ndi Imam Abu Yusuf ndi Imam Muhammad. Pomwe Madhhab a Maliki ndi Shafii akuti ndi Sunnah [Ndi zololedwa kwa munthu wotsanzira Madhhab a Maliki kusiya Witr ngati pali haraj (zovuta zomwe zafotokozedwa ndi Chisilamu).]

Takbir-i-iftitah imakwanilitsidwa ndi amuna kukweza manja awo kufika ku makutu awo komanso ndi kukhala tcheru mu mtima.

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti Qiyam ikwaniritsidwe: Kuyima moyang'ana ku Qibla, maso adziyang'ana pa malo a sajda, (pomwe uyika chipumi chako ndi nsonga ya mphuno yako pogwada) ndi kusagwedezeka pa nthawi ya Qiyam.

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti Qiraat ikwaniritsidwe: Kusoma ma surah (ayah) mokweza pamene ayenera kuchitidwa mokweza, komanso monong'ona moti udzimva mawu ako pamene ayenera kuchitika monong'ona ndi kutchula mawu molondola. Kuganizira matanthauzo a Qur'an al-kareem yomwe mukuwerenga. Kusunga malamulo a tajwid pamene mukuwerenga ma ayah. Chitani namaz ndi china chirichonse chowerengedwa mu Namaz ndi azan mu chiyankhulo cha Chiarabu. Phunzirani kuwerenga mawu a Chiarabu moyenera kuchokera kwa hafiz wodziwa Chisilamu ndipo yemwe amatsatira malamulo omwe anenedwa m'mabuku a ilmihal a Madhhab awo. Ma ayah a Qur'an al-kareem olembedwa mu zilembo za Chilatini sangawerengedwe molondola. Kuwerenga kochokera m'menemo kudzakhala kolakwika. Tafsir (kufotokozera) kwa Qur'an al-kareem ndi kutheka. Kutanthauzira ndiye ayi. Mabuku omwe

abweretsedwa m'dzina la Qur'an yotanthauziridwa mu ziyankhulo zina olembedwa ndi anthu opanda chipembezo komanso opanda madhhab ndi olakwika. Ndi osakhonza komanso ndi osalondola. Msilamu aliyense ayenera kuphunzira Qur'an al-kareem. Phunzirani zilembo za Chisilamu, kuti muthe kuwerenga ndi kulakatula Qur'an al-kareem ndi mapemphero molondola. Namaz yochitika powerenga ma ayah ndi mapemphero molondola idzalandiridwa. Zanenedwa motere m'buku la **Targhib-us-salat**: "Ngati ma ayah ndi mapemphero owerengedwa mu Namaz ndi munthu ali osalondola malinga ndi akatswiri a Chisilamu asanu ndi anayi (9) koma ndi olondola malinga ndi katswiri m'modzi, namaz yachitikayo siyingakhale fasid."] (Kupembedza komwe kuli fasid ndi komwe sikunalandiridwe.)

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti ruku ikwaniritsidwe: Kuchita ruku poyang'ana ku Qibla, kuŵerama molondola powerama ngati chilembo chachikulu cha 'L' chitatembenuzika.) Chiwuno ndi mutu zikhale pa mlingo imodzi. Kukhala pa ruku kwa kanthawi (tumaninat), [mpaka mtima wanu utakhutitsidwa.]

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti sajda itheke: Kuwerama pa sajda m'njira yolamulidwa ndi Sunnah. Kuchita sajda molunjika ku Qible, pogunditsa chipumi ndi mphuno pansi molunjikana. Kukhala pa sajda kwa kanthawi kuti mukwaniritse tumaninat. [Ndi zololedwa kwa munthu wathanzi kupanga sajda pa chinthu chotalika mpaka masentimita makumi awiri ndi asanu (25) kuchokera pansi (pomwe akuchitira namaz), komabe kutero ndi makruh. Zili choncho chifukwa Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" sadachitepo sajda pa chinthu choti ndi chotalikirapo; ngakhale Ashab-i-kirim sanapangepo. Kuchita sajda pa chinthu chotalikira kungachititse kuti namaz ikhale fasid.]

Pali zinthu zitatu zofunikira kuti qa'da-i-akhira itheke: 1– Kwa amuna kukhalira phazi la kumanzere ndi kuyimika phazi la kumanja, ndipo akazi kukhala m'njira yotchedwa tawarruk –komwe ndi kukhalira matako ndipo mapazi atulukire kumanja. 2- Kuwerenga pemphero la Tahiyyat molemekeza. 3- Pa qa'da-i-akhira (kukhala komaliza), kunena Salawat ndi mapemphero ena olongosoledwa. Ma dua onenedwa pamapeto kwa Namaz aphunzitsidwa mtsogolomu.

GHUSL (KUSAMBA)

Pali ma farze atatu (3) oti mutsate popanga ghusl malinga ndi Madhhab a Hanafi; ma farze asanu (5) malinga ndi Madhhab a Maliki;

ma farze awiri (2) malinga ndi Madhhab Shafi'i, ndi farze imodzi (1) malinga ndi Madhhab Hanbali. M'Madhhab a Hanafi:

1– Kutsuka mkamwa kamodzi ndi madzi. Ndi fardh kunyowetsa pakati pa mano ndi mkati mwa mipata ya mano. [Msilamu yemwe amatsata Madhhab a Hanafi sangamatitse mano kapena kuyikitsa ma karawuni, pokhapokha pali darurat kuti atero. Atha kuyikitsa mano omachotsa kuti azitha kuchotsa ndikutsuka pansi pake pochita ghusl. Msilamu okhala ndi mano omata kapena ali ndi karawuni popanda darurat adzakhala Msilamu wokhala ndi udhr chifukwa cha haraj (zovuta) zomwe wakumana nazo; adzayenera kutsata pakati pa Madhhab a Shafi'i kapena Maliki popanga ghusl. Zikatero, adzayenera kuwonjezera mau akuti, "Ndikutsata Madhhab a Shafi'i kapena Maliki" pa niyyah yawo nthawi iliyonse akamasamba ndi pochita namaz.]

2– Kuthira madzi m'mphuno kamodzi.

3- Kusamba thupi lonse kamodzi. Ndi fardh kusambitsa ziwalo za thupi zomwe sizingayambitsa haraj (mavuto) zitasambitsidwa. Ngati chiwalo cha pa thupi sichingathe kusambitsidwa chifukwa cha darurat, mwachitsanzo chibadwa osati chochita munthu kuchipanga yekha, Allahu ta'âlâ adzakhululuka ndipo ghusl yochitikayo idzakhala sahih (yokwanila).

Monga momwe zafotokozedwera m'bukhu lotchedwa **Durr-ul-mukhtar**, chakudya chotsalira pakati pa mano kapena m'mipata ya mano sichingalepheretse ghusl kukhala sahih. Zili choncho malingana ndi fatwa.[1] Poti madzi adzalowerera ndi kunyowetsa malo a kunsi kwawo. Akatswiriwo akuti ngati zotsalirazo ziri zolimba, zingalepheretse madzi kulowamo. Ndipo izi ndi zowona zake. **Ibni 'Abidin** "rahima-hullâhu ta'âlâ" akufotokoza nkhaniyi motere: Zalembedwa m'bukhu lotchedwa **Khulasa-t-ulfatawa**, kuti zimenezo sizingalepheretse madzi kulowerera chifukwa madzi amayenderera ndipo adzadutsa chakudyacho mosavuta mpaka kukanyowetsa malo apansi pake. Ngati kutapezeka kuti madzi sakudutsa mu zakudya zotsalira, ghusl yochitikayo siidzakhala sahih. Izi amavomereza akatswiri onse mogwirizana. Zomwezo zanenedwanso m'bukhu lotchedwa **Hilya-t-ul-mujalli**, lolembedwa ndi Ibni Emir Hajj Halabi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", 879 (1474 AD). Ngati zotsalira za chakudya zalimba, madzi sangadutse ndipo ghusl yopangidwa siyidzakhala

[1] Fatwa ndi kulongosola komaliza komwe katswiri wa chiphunzitso cha Chisilamu wovomerezeka amayankha mafunso a Asilamu pankhani yachipembedzo. Magwero ndi mfundo zomwe zagwiritsidwa ntchito pofika pa fatwa zimawonjezeredwa ku fatwa.

sahih. Zikatero palibe darurat [kunena kuti, sichinthu chimwe chachitika chokha.] Ndipo palibe haraj posambitsa mbali imeneyo.

Zalembedwa m'bukhu lotchedwa **Halabi-i-saghir**: Ngati munthu wachita ghusl ali ndi zotsalira za buledi kapena chakudya kapena zinthu zina pakati pa mano ake, ghusl yake idzakhala sahih, malingana ndi ma fatwa, ngakhale iye ataganiza kuti madzi amasambawo sanadutse mu zotsaliramo. Fatwa yoperekedwayi ikugwirizana ndi zomwe zalembedwa mu **Khulasat-ul-fatawa**. Malinga ndi kunena kwa akatswiri ena ghusl yochitikayo siyidzakhala sahih ngati zotsalirazo ziri zolimba.

Chigamulo chomalizachi chalembedwanso m'bukhu lotchedwa **Zahirat-ul-fatawa**, (lolembedwa ndi Burhanaddin Mahmud bin Tajuddin Ahmad bin 'Abd-ul-'Aziz Bukhari "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", 551 [1156 AD] yemwe anaphedwa mu 616 [1219].) Ndi chigamulo cholondola pa nkhaniyi. Poti madzi sangalowe kufika pansi pa zotsalirazo za zakudyazo. Ndipo palibe daruat kapena haraj.

M'buku lotchedwa **Durr-ul-Muntaqa**[1] zanenedwa motere. Pa ghusl yochitika chakudya chitatsalira m'mipata ya mano anu, akatswiri a Chisilamu ena amatsutsa kuti ghusl yotere idzakhala sahih. Komanso pali ena amakhulupilira kuti siyidzakhala sahih. Pofuna kuchotsa chikayikiko, chakudya chitsalira m'mano chiyenera kuchotsedwa kaye musanayambe ghusl. Monga zafotokozedwera mu **Tahtawi** pa ndemanga ya **Maraq-il-falah,** kuti: ngati chakudya chatsalira m'mabowo a mano kapena pakati pa mano, ghusl idzakhala sahih. Pakuti madzi amayendelera ndipo amadutsa paliponse mosavuta. Ngati zotsalira za chakudya zalimba ndi kutafuna, chakudyacho chidzachinga ghusl. Zalembedwanso m'bukhu lotchedwa **Fath-ul-qadir.**

Zanenedwa m'bukhu lotchedwa **Bahr-ur-raiq** kuti ghusl idzakhalabe sahih ngakhale pali chakudya chatsalira m'mano kapena pakati pa mano chifukwa madzi ndi chinthu chabwino kwambiri chomwe chimadutsa mu chilichonse. Izi zalembedwa m'bukhu lotchedwa **Tajnis**. Koma Sadr-ush-shehid Husamaddin ananena kuti ghusl yochitika motere siyidzakhala sahih ndi chifukwa chake kuli koyenera kuchotsa chakudya chotsalira kuti madzi ayende mkati mwa dzino. Ndi kwabwino kuchotsa zotsalira ndikutsuka kunsi kwa mano.

[1] Yolembedwa ndi 'Alauddin Haskafi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (1021, Haskaf – 1088 [1677 A.D.]).

M’bukhu la **Fatawa-i-Hindiyya** zanenedwa kuti: Pa mtsutsowo, zonena kuti ghusl yochitika ndi munthu amene chakudya chatsalira mmano kapena pakati pa mano ake ndi sahih ndizo zikuyandikira ku chowonadi. Zomwezo walembedwa mu **Zahidi**. Koma ndi bwino kuchotsa zotsalirazo ndikuyesetsa kuti madzi alowe mmipatamo. Monga zafotokozeredwa m’bukhu lotchedwa **Qadikhan**, zalembedwanso m’buku lotchedwa **Natifi** kuti ghusl yopangidwa pomwe pali zotsalira za chakudya zitazungulira mano siyingachitike mokwanira ndipo ndi kofunika kuchotsa ndi kutsuka malo omwe ali pansi pake.

Kwalembedwa m’bukhu lotchedwa **al-Mejmu’at-uz-zuhdiyya** kuti: Ngati zotsalira za chakudya zili pakati pa mano chidzakhala ngati chi nsima cholimba ndipo chidza chinga madzi kuti asalowe pansi pa dzino. Ngakhale zakudyazo zili zochepa, zimalepheretsanso ghusl. Zonga izi zalembedwa mu **Halabi**. Ndizachiziwikire kuti kuchotsa zotsalira za chakudya mmano ndi kosavuta. "palibe haraj, pochotsa zotsalira za chakudya mmano. Koma mano omata ndi ovala sangangachotsedwe; choncho pali haraj kuchotsa.” Inde, pali haraj. Koma kumata mano ndi zochitika zofuna munthu choncho sichingakhale haraj. Zimakhala udhr kwa iye potsatira Madhhab ena. Sizikhala udhr kusiya fardh. Munthu kukhululukidwa ku fardh kuyenera kuti palibe Madhhab ena oti ndi kutsatira. Izi zikutanthauza kukumana pa mmodzi kwa darurat ndi haraj.

Zikhonza kufunsidwe kuti, “Poti cholinga chomatitsira mano kapena kuvala karauni ndi kupewa ululu wa kuwawa kwa mano komanso kuwateteza kuti asawole, ndiye palibe darurat yoti ndi kukhululukidwa ku fardh posatsuka zitsulo za m’mano)?” Yankho lathu lidzakhala motere: “kuti pakhale darurat kumafunika kuti pasakhale njira yina monga kutsanzira Madhhab ena.”

Mtsutso woti, "Udindo wotsuka mano pochita ghusl umashuntha ndi kupita kunja kwa zomatazo kapena karawuni" si oyenera mu Chisilamu. Tahtawi Ahmad bin Muhammad bin Isma’il akunena m’kulongosola kwake za bukhu la Shernblali lotchedwa **Imdad-ul-Fattah** akuti: “Munthu akapanga udhu ndi kuvala zonyansa atamaliza kupanga udhu, udhu wake umawononge ka. Kuonongekako kumakhudza zonyansa m’malo mwa mapazi.” Khulankhula uku m’mabuku a Fiqh kukhudza udhu ndi kuvala zonyansa. Kuwakonza kuti agwirizane ndi zochitika zokhudza kuvala mano ndi kuchita ghusl, kumatanthauza kuperewera nzeru ndi kupereka ma fatwa a mmaganizo a munthu. Sikungakhale koyenera kuyerekeza dzino

lomata kapena lovala ndi ndevu zochuluka. Poti sikokakamizidwa kusambitsa khungu pansi pa ndevu posamba. Munthu amene amatsutsa kuti si fardh "kutsuka khungu la pansi pa ndevu posamba poti si fardh kutsuka khungu la pansi pa ndevu pochita udhu" sadzatsuka khungu la pansi pa ndevu. Potero ghusl yochitika ndi munthu ameneyo ndi anthu amene amamukhulupilira, ndi kutsata mapemphero a Namaz omwe akuwachita, siidzakhala sahih.

Komanso sizingakhale zogwirizana ndi mabuku a Fiqh kufananiza kumata mano ndi mafuta odzola opaka pa ming'alu ya mapazi kapena ndi timatabwa tomangilira ziwalo zovulala kapena zosweka kapena chikhakha choikidwa ngati mabandeji.

Poti pakakhala haraj kapena kuwonongeka komwe kungadze pochotsa pa mabala ndi ziwalo zothyoka, sizingatheke kutsanzira Madhhab ena. Pa zifukwa zitatu izi, munthu adzaloledwa kuti asatsuke pansi pake.

Muli ndi ufulu wosankha kumatitsa dzino lovunda ndi lopweteka kapena kuvala karauni chifukwa simukufuna kuchotsetsa ndi kuyika dzino labodza lomachotsa kapena mano onyenga okhala ndi theka la nkhama mkamwa monse. Kumatitsa mano anu kapena kuvala karauni kapena kukhala ndi mlatho wokhazikika wa mano sikungabweretse darurat. Kunena kuti pali darurat, payokha, sikungachititse kukhala chifukwa chokukhululukirani kuti musatsuke pansi pa maderawa. Poti ndi kotheka kutsanzira Madhhab ena. Palibe amene ali ndi ufulu wogwiritsa ntchito mkangano wopanda maziko woti pali darurat ngati chida chonyozera anthu ena, omwe amamvera mabuku a Fiqh ndikutengera ma Madhhab a Shafi'i kapena Maliki.

Darurat amatanthauza chinthu chosayembekezeka chimene chimankakamiza munthu kuchita china chake kapena kusachita china chake choyenera kuchita. Zitsanzo za darurat ndi malamulo a Chisilamu ndi zoletsedwa zake, kupweteka kowopsa, ngozi yotaya chiwalo chimodzi kapena moyo wa munthu, komanso kukhala wopanda njira ina. **Haraj** ikutanthauza vuto kapena chiphyinjo chomwe chingaletse chinthu chomwe wachita kukulepheretsa kuchita chinthu chomwe chili fardh kapena kukuchititsa kuchita chinthu cha haramu. Malamulo ndi zoletsedwa za Allahu ta'âlâ, zikasonkhanitsidwa pamodzi, zimatchedwa **Ahkam Al-islamiyya**. Posunga limodzi mwa malamulo a Ahkam Al-islamiyya, monga kuchita limodzi mwa malamulo kapena kupewa chimodzi mwa zolesedwa, mumatsatira mawu odziwika ndi osankhika omwe amanenedwa ndi akatswiri a m'Madhhab anuwo okhudza nkhaniyo. Ngati haraj (vuta)

kutsatira mawu osankhidwa aukatswiri liwoneka chifukwa cha zomwe mwachita, tsatirani za akatswiri ena omwe ali ofewako omwe ali mu Madhhab anu. Ngati pali haraj kutsatira mawu a wachiwiriyo, ndiye kuti mutsatire Madhhab ena ndipo tsatirani Madhhab amenewo pa nkhaniyo. Ngati pali haraj kutsatiranso Madhhab enawo, ndiye kuti muyang'ane pa nkhaniyo ngati pali darurat kapena ayi pa kuchita chinthu choyambitsa haraj:

1- Ngati pali darurat pochita chinthu cha fardh yomwe ikubweretsa haraj, inu mudzakhululukidwa kusachita fardh.

2- Ngati palibe darurat pochita chinthu yomwe ingayambitse haraj, [monga kupukuta zikhadabo,] kapena pali darurat koma pali njira zingapo zochitira chinthucho ndipo iwe ndikusankha njira yomwe ingadzetse haraj, ntchito yopembedza yomwe ukuchita m'njira yodzetsa haraj siyidzakhala sahih. Muyenera kuchita fardh pogwiritsa ntchito njira yopanda haraj. Zalembedwa kuti mutha kutsatira Madhhab ena ngati pali haraj, (kutanthauza kuti ngati mwasankha njira yomwe ili ndi haraj) posatengera kuti pali darurat kapena ayi. Izi zalembedwa m'mabuku awa: **Fatawal-hadithiyya** (lolembedwa ndi Ibn-i-Hajar-i-Makki "rahmatullâhi 'alaih", 899 [1494 AD] - 974 [1566], Makka); **Khulasat-ut-tahqiq** (lolemba ndi Abd-ul-Ghani Nablusi "rahmatullâhi 'alaih" , 1050 [1640 AD], Damuscus - 1143 [1731],) mu Tahtawi's "rahima-hullâhu ta'âlâ" pa mawu a Sharblali "rahima-hullâhu ta'âlâ" m'bukhu la **Meraq-il-felaht** komanso m'bukhu la **Ma'fuwat** olembedwa ndi Halil Es'irdi "rahima-hullâhu ta'âlâ", yemwe anamwalira mu 1259 [1843 A.D.]. Msilamu wa Hanafi yemwe akumatitsa mano ake opweteka kapena ovunda kapena kuti avale karauni m'malo mochotsa ndi kuyikapo mano abodza kapena mano opangidwa ndi nkhama zomwe, ayenera kutsanzira Madhhab a Shafi'i kapena Maliki pamene akupanga ghusl. M'Madhhab awiriwa si fardh kutsuka mkamwa ndi mphuno popanga ghusl. Ndipo ndikosavuta kutsatira Madhhab a Shafi'i kapena Maliki. Koma muyenera kuchita niyyah, mu mtima mwanu, kuti mukutsatira Madhhab a Shafi'i kapena Maliki pamene mukuchita ghusl, kuchita udhu kapena kuchita Namaz. Ngati mwaiwala, chitani pomwe mwakumbukira ngakale muthamaliza Namaz yanu. Potero, udhu wanu ndi ghusl yomwe mukuchita komanso Namaz yomwe mukupemphera, zikuyenera kukhala za sahih (zovomerezeka) malingana ndi Madhhab Shafi'i kapena Maliki. Potsatira Madhhab a Shafi'i, kuti udhu ukhale sahih, ndi kofunika kuchitanso udhu wako ukakhudza khungu la mkazi kupatula akazi khumi ndi asanu ndi atatu (18) omwe ali Haramu kwa muyaya kwa inu

kuchita nawo nikah. Ndikofinikanso kubwereza udhu ngati dzanja la kumanja lanu lakhudza qaba awrat (maliseche) anu. Ngati mukuchit namaz yotsogozedwa ndi imam (jamaat), werengani Surah Fatiha cha mumtima. Chonde onani mutu wachisanu ndi chimodzi gawo la chinayi la m'bukhu la **Endless Bliss** kuti mudziwe zomwe muyenera kuchita potengera Madhhab a Maliki! Kutsatira Madhhab ena sikutanthauza mukusintha Madhhab anu.

Msilamu wa Hanafi yemwe akutsatira Madhhab ena sanatuluke m'Madhhab a Hanafi. Amatsata Madhhab amenewo m'ma fardh ndi mufsid. Amasunga malamulo a Madhhab ake mu wajib, makruh, ndi Sunnah.

Zonena za akatswiri a Fiqh zokhudza ghusl zilipobe pofuna kuyesa kuthetsa funso la mano ndi zolemba za anthu osazindikira omwe satsata Madhahab aliwonse. Iwo kuti zanenedwa mu fatwa yolembedwa mu 1332 [1913 A.D.] yoperekedwa m'periodical yotchedwa Sebil-ur-rashad kuti nkololedwa kumata dzino. Tikufuna kunena poyamba kuti zolembedwa zotchedwa periodical ndi nkhani zolembedwa ndi omwe amati akukhonza chipembezo ndipo satsatira Madhhab aliwonse. M'modzi mwa olemba amenewa Isma'il Hakki waku Manastir (Bitola), yemwe ndi wachinyengo wa freemason. Wina ndi Isma'il Hakki waku Izmir, yemwe ali patsogolo pa zitsiru zomwe zidasokonezedwa ndi Mehmet Abduh, mufti wa masonic waku Cairo yemwe amati wokhonzanso Chisilamu. Anachita maphunziro a kusekondale ku Izmir ndipo anamaliza sukulu ya uphunzitsi ku Istanbul. Maphunziro ake a chipembedzo ndi ofowoka ndipo alibe kuzindikira pa za chipembedzo. Mothandizidwa ndi a chipani cha Union, anakhala mphunzitsi wa madrasa ndikuyesa kufalitsa malingaliro a Abduh osintha zinthu komanso osokoneza. Mawu oyamikira amene Isma'il Hakki analemba m'buku lotchedwa Telfiq-i-madhahib, akusonyeza mkwiyo wake wamkati. Telfiq-i-madhahib ndi tanthauzo kuchokera kwa Rashid Rida wa ku Aigupto ndipo lonamasuliridwa ndi Ahmed Hamdi Akseki, mmodzi mwa ophunzira ake amene anazunzidwa ndi chinyengo chake chaukali.

Isma'il Hakki yemweyonso anakulitsa mkangano pakati pa akatswiri a Fiqh pa nkhani yomanga mano ndi waya wa golide. Anatulutsa mabuku kuperekera ndemanga pa bukhu la Muhammad Shaybani lotchedwa **Siyar-i-kebir**, lomwe likulongosola zoti a katswiri pa nkhaniyi anagwirizana kuti pali darurat kumanga mano ndi waya wa golide mmalo mwa waya wa siliva. Koma, funso lomwe adafunsidwa linali loti ghusl yochitika ndi munthu wokhala ndi dzino lomata kapena

ovala karauni ili sahih, osati zomanga mano ndi waya wa golide kapena siliva. Polemba zambiri kulongosoka nkhani yomwe sanafunsidwe komanso yomwe choona chake chimadziwika ndi kale, munthu uyu witchedwa Isma'il Hakki wa ku Izmir analemba anasokoneza ndikukhala ngati zomwe analemba iye ndiye zowona zenizeni. Zomwe anachita ndi upandu ndi bodza chabe zongofuna kusokoneza choonadi. Uwu unali ukatyali wolemba maganizo ake pobisala mu fatwa yoperekedwa ndi akatswiri a Chisilamu.

Ukatyali wake ndi woyipa kwambiri. Amagwiritsa ntchito mawu olembedwa ndi akatswiri a Fiqh pa ghusl pokwaniritsa zofuna zake. Mwachitsanzo, iye anati: "Monga zanenedwera mu **Bahr**, sikokakamizidwa kufikitsa madzi m'malo omwe ali ovuta kufikamo". Koma bukhu la Bahr likuta: "…ziwalo za thupi zimene zimakhala zovuta kuti madzi afike" Mutha kuona kuchokera mziganizo ziwirizi kuti iye amayerekezera chinthu chomwe munthu amachita kwambiri ndi chinthu chomwe munthu amakumana nacho kwambiri. Komanso sakunena zoona pogwiritsa ntchito mawu akuti, "Ngati kungakhale kowawa mkazi kusamba m'mutu, ndiye kuti asatsuke m'mutu mwake," zomwe zinalembedwa mu **Durr-ul-mukhtar** ngati umboni woti ghusl yochitika ndi munthu woti wamata dzino idzakhala jaiz (yololedwa, yovomerezeka). Ululu m'mutu mutatiridwa madzi ndi matenda akuthupi. Kuveka dzino karauni kapena kumata ndi chisankho cha munthu. Ndi chifukwa chake nkhani yoti ghusl yochitika ndi munthu yemwe ali ndi zotsalira za chakudya m'mano mwawo ili jaiz ikufotokozedwa pa yokha m'buku lotchedwa **Durr-ul-mukhtar.**

Ukathyali ndi zochita zoyipa zomwe zatchulidwa pano zikucheperabe kufotokoza kuyipa kwa Isma'il Hakki wa ku Izmir. Mwachitsanzo, analibe mfundo zokwanira zoonetsa kutsutsa ma umboni akatswiri a Chisilamu ponena kuti, "Ndizosafunika popanga ghusl kuti madzi afike pansi pa karauni ya golide ndi siliva kapena kutsuka malo pansi pawo. Akatswiri a Fiqh amavomerezana kuti pali darurat pa dzino lokhudzidwalo kotero kuti sikokakamizidwa kufikitsa madzi ku ziwalo (za thupi) zomwe zili darurat."

Palibe ndi mmodzi yemwe mwa akatswiri a Fiqh m'Madhhab a Hanafi amene ananena kuti ndi darurat kuvala makaraun kapena kumata mano. Zowona zake ndi zoti, kukongoletsa mano kapena kumata mano sizinayambike kale. Pa nthawi ya akatswiri a Fiqh zimenezi kunalibe. Pa tsamba la makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zinayi (64) la ndemanga pa bukhu lotchedwa **Siyar-i-kebir**, lomwe likuperekedwa ngati umboni, Imam Muhammad Shaybani

“rahima-hullâhu ta’âlâ” watchulidwa kuti anati ndi jaiz (zololedwa) kuti munthu kuyike dzino la golide pa malo omwe dzino lake lagwa kapena kumanga ndi mawaya a golide. Bukhuli silinatchulepo za karauni wa mano. Izi ndi zopeka, zongowonjezera za Isma'il Hakki waku Izmir.

Amuna achipembedzo cha Masonic, anthu opanda Madhhab odziwika bwino ndi ampatuko, omwe analipo pambuyo pa akatswiriwa anagwiritsa ntchito chinyengo chamtundu uliwonse kuwanyenga Asilamu ndi kuwalalikira za mpatuko pakati pawo. Analemba zinthu zolakwika komanso zosokoneza.

Imam Muhammad Shaybani “rahima-hullâhu ta’âlâ” ananena kuti dzino losweka likhoza kumangidwa ndi waya wa golide kapena wa siliva. Iye sananene kuti idzakhala jaiz kuyika karauni kapena kumata ndi golide. Zinthu zotere zabzalidwa ndi Isma’il Hakki ndi ena otero.

Ma mufti ndi anthu ena ofunikira m’chipembedzo a nthaŵi ya Isma’il Hakki wa ku Izmir anapereka mayankho ndi cholinga choulula chowonadi motsutsana ndi nkhani yabodza ndi yonyenga imene takamba m’ndime zam’mbuyomu. Mmodzi mwa akatswiri owerengeka amenewo ndi Yunus-zade Ahmed Vehbi Efendi wa ku Bolvadin, Turkey, “rahima-hullâhu ta’âlâ”. Munthu wophunzira mozama uyu yemwe anali ndi kuzindikira kochuluka kwa chipembedzo anatsimikiza kuti akatswiri a Chisilamu adagwirizana kuti ghusl yochitika ndi munthu womata zitsulo siyingakhale sahih.

Osindikiza magazini otchedwa **Sebil-ur-rashad** anali a nzeru pa chinyengo. Amagwiritsa ntchito nkhani zacbodza zachiziwikire zopekedwa ndi lembedwa ndi Izmirer, kotero kuti anawona kuti ndikofunikira kuthandizira nkhanizo ndi umboni wina powonjezerapo fatwa ndi mawu omaliza akuti, “... ghuslyo idzakhala sahih,” mu kusindikiza kwachiwiri mchaka cha 1329 [1911 AD], kwa bukhu la fatwas lotchedwa **Majmu'ai-Jedida**. Koma, fatwa ikunenedwayo mulibe mu kusindikidza koyamba, kwa chaka cha1299 A.H. m’bukhuli. Mawu osokonezawa anayikidwa mu kusindikiza kwa chiwiri ndi Musa Kazim, shaikh-ul-islam yemwe anayikidwa pa udindo ndi chipani choipa cha Union. Chotero, magazini ya Sebil-ur-Rashad inayesa kuwonjezera mawu amene anapangidwa ndi ma freemason kuti agwirizane ndi nkhani yolembedwa ndi wobweretsa zinthu zatsopano mu Chisilamu.

Palibe wophunzira ndi m'modzi yemwe wa Fiqh amene ananena za 'darurat' ya karauni kapena kumata mano. Anthu omwe akunena kapena kulemba choncho ndi achipembedzo cha masonic kapena

magulu ozitcha okonzanso Chisilamu kapena anthu opanda Madhhab ena kapena anthu osadziwa Chisilamu omwe anamizidwa kapena kunyengedwa ndi ampatuko a Wahhabi, ndipo palibe wina koma iwo.

Ahmad bin Muhammad bin Isma'il Tahtawi “rahima-hullâhu ta’âlâ” akunena motere m'mawu ake m’bukhu la Shernblali lotchedwa **Meraq-il-falah**: "Pamene mukupemphera mu jama'at potsatira imam yemwe ali mu amodzi mwa Madhhab ena atatu, Namaz yomwe mukuchita idzakhala Sahih ngati pa imamu akutsogolerayo palibe chinthu chomwe chimaononga Namaz malinga ndi Madhhab anu, ngakhale chiri chosawongonga namazi m’madhhab a imamuyo. Koma ngati chilipo, inu musadziwe za icho pomwe mukumutsatira. Iyi ndiye qawl (umboni) wodalirika kwambiri. Malingana ndi qawl (umboni) wina, ngati Namaz ya imam ili sahih molingana ndi Madhhab ake, kudzakhala sahih kumutsatira ngakhale kuti namazi yakeyo siili sahih malinga ndi Madhhab anu.” Lamulo lomweli lalembedwa mu Ibni Abidin.

Mmene zikumvekera kuchokera m’mawu awa omwe adalembedwa mu ndemanga ya Tahtawi komanso mu Tahtawi “rahima-hullâhu ta’âlâ”, pali ma qawl awiri osiyana okhudzana ndi Namaz yochitidwa ndi msilamu wa Hanafi yemwe alibe ma karauni kapena mano omata koma akutsogozendwa ndi imam yemwe ali ndi ma karauni kapena mano omata: Malinga ndi qawl yoyambayo, sizili sahih kwa Msilamu wa Hanafi wosavala ma karauni kapena osamata mano kutsatira imam wovala karauni kapena wa mano omatidwa. Poti, namaz ya imam ameneyo si sahih malinga ndi Madhhab Hanafi. Potengera qawl yachiwiriyo, ngati imam akutsata Madhhab a Shafi'i kapena Maliki, zidzakhala sahih kwa Asilamu a Hanafi osamata mano kapena kuvala karauni kumutsatire; kupemphera namaz ya jama'at yoaogozedwa ndi iye.) Iyi ndi ijtihad (chigamulo) cha Imam Hinduwani “rahmatullâhi ’alaih”. Lamulo lomweli likugwiranso ntchito m’Madhhab a Shafi’i. Pokhapokha zitadziwika kuti imam yemwe ndi wa Salih wokhala ndi mano oveka kapena omata sakutsanzira Madhhab a Maliki kapena Shafi'I, Asilamu a Hanafi omwe alibe mano a kalauni kapena omata akuyenera kuchita namaz mu jama'at yotsogozedwa ndi imam ameneyo. Nkosaloledwa kumufunsa ngati akutsanzira Madhhab a Maliki kapena Shafi’i popemphera. Qawl yachiwiriyi ndi yofowoka. Koma monga tanenera kale m’ndimeyi, pakakhala haraj (zovuta), ndi kofunika kutsata qawl yofooka. Zoti qawl yofowoka ichitike pofuna kupewa fitna zalembedwanso mu **Hadiqa**. Ngati munthu anyoza Madhhab anayiwa ndikuchita mapemphero ake m’njira yosagwirizana

ndi chiphunzitso cholembedwa m'mabuku a Fiqh, zidzatsimikizika kuti iye si wa Sunni. Ndipo munthu yemwe sali wa Sunni ndiye kuti ndi wa bidah komanso wapatuka, kapena wopanda iman ndipo amakhala murtadd (wogalukira). Sitikunena kuti musamatitse mano kapena kuveka karauni. Tikungofuna kuwaonetsa abale ndi alongo athu amene anamatitsa mano awo kapena kuwaveka karauni njira zo-lambira zovomerezeka. Tikuwawonetsa njira zosavuta.

Pali mitundu khumi ndi isanu (15) ya ma ghusl (zifukwa zokupangisani kusambira): isanu mwa iyo ndi fardh, isanu mwa iyo ndi wajib, inayi ndi Sunnah, ndipo umodzi mwa iyo ndi mustahab. Ma Ghusl omwe ali fardh: Mkazi kapena mtsikana akamaliza nsambo kapena nthawi yobereka ikatha; pakutha pa kugonana; mukatulutsa umuna/ikazi mwa chikhumbo; kuzilotera ndi kuona umuna kapena ukazi pa bed kapena m'kabudula wamkati. Ndi fardh kuchita ghusl nthawi ya Namaz isanathe.

Ma Ghusl awa ali wajib: Kusambitsa Msilamu wakufa. Mwana akangotha msinkhu achite ghusl. Mwamuna ndi mkazi wake akadzuka atagona limodzi ndi nkuona madzi otuluka mnthupi pakati pawo koma osadziwa kuti zatuluka mnthupi la ndani, zili wajib kwa onse awiri kuchita ghusl. Ukaona madontho a umuna koma suukukumbukira nthawi yomwe unakodza, ndiye kuti kuchita ghusl ndi wajib. Ndipo mkazi akabereka mwana, zili zoyenera kwa iye kuchita ghusl ngakhale palibe kutaya magazi. (Ndi fardh kuchita ghusl ngati patatuluka magazi.)

Ma ghusl omwe ali Sunnah ndi awa: Ghusl popita ku Jummah ndi masiku a Eid; nthawi ya Ihram (pokachita haji kapena umra)- ndinso musanakwere pa (phiri la) Arafat .

Ghusl yomwe ili mustahab: Osakhulupilira akavomera ndikukhala okhulupilira. Ngat iye anali ndi Janaba asanakhale Msilamu, zili -fardh kwa iye kuchita ghusl.

Pali ma haram atatu pa ghusl:

1– Kwa onse, amuna ndi akazi kuonetsa matupi awo a pakati pa mchombo ndi mawondo kwa anthu ena pochita ghusl. Ndi haram muna kuwonetsa ziwalo za thupi lake kuyambira pa mchombo mpaka pansi pa mawondo kwa amuna ena, komanso mkazi kuwonetsa akazi anzake ziwalo zawo pakati pa mchombo ndi mawondo pa nthawi imene akuchita ghusl.

2- Malinga ndi qawl, ndi haram kwa akazi a Chisilamu kudzionetsa kwa akazi omwe sali Asilamu pochita ghusl. (Lamuloli liyenera kutsatiridwa nthawi ina iliyonse.)

3- Kusakaza madzi ndi haram. Ndi koletsedwa kugwiritsa ntchito madzi ochulukira mosasamala pochita ghusl.

Mu Madhhab a Hanafi, muli ma Sunnah khumi ndi atatu (13) oti azitsatiridwa pochita ghusl:

1- Kuchita istinja ndi madzi. Komwe ndi kudzitsuka utakodza kapena kunyera, kutsuka potulukira mphweya ndi kumaliseche.

2– Kusamba m'manja mpaka polumikizira dzanja.

3- Ngati pa thupi pali najasat (nyansi) yeniyeni, kuyichotsa.

4- Kukhala tcheru kwambiri pochita mazmaza ndi istinshaq. (mawu oti Mazmaza amatanthauza kuchukucha mkamwa ndi madzi, ndipo istinshaq amatanthauza kulowetsa ndi kutulutsa madzi m'mphuno.) Ghusl siidzakhala sahih (yokwanira) ngati pali malo osanyowa m'kamwa kapena m'mphuno (ngakhale atakhala ochepa ngati nsonga ya singano). Kuchita wudhu ngati okachita namaz musanayambe ghusl.

5- Kuchita niyyah pochita ghusl.

6- Kutikita chiwalo chilichonse chomwe chathiridwa madzi, ndi manja.

7- Kuyamba kuzithira madzi pa mutu, kenako pa phewa la dzanja la manja ndi la manzere, paliponse katatu.

8- Kuchita khilal pakati pa zala za mmanja ndi zala za kuphazi. Uku ndi kutsuka pakati pa zala za mmanja ndi zala za kuphazi.

9- Osayang'ana kapena kapena kuonetsa mbuyo yanu ku Qibla.

10- Osayankhula zinthu za pa dziko pochita ghusl.

11- Kuchita mazmaza ndi istinshaq katatu.

12- Kusambitsa chiwalo chirichonse kuyambira kumanja.

13- Kusakodzera pa malo pomwe mukuchitira ghusl madzi omwe mukupangira ghusl sakuyenda. Palinso ma Sunnah ena kuwonjezera pa ma Sunnah tatchulawa.

PEMPHERO LA TAWHID

Yaa Allah Yaa Allah, Laa ilaaha illaallah Muhammadun Rasoolullah. Yaa Rahmaan Yaa Raheem, Yaa Afuwwu Yaa Kareem, fa'afu annee, warhamnee Yaa Ar'ham Rahmeen! Tawwafanee Musliman wa al-hiqnee bi-ssaliheen, Allahumma ighfirilee wal-abaai wa ummahaati wal-abaai wa ummahaati zawjaati wal-ajadaad wa jaddati wal-abnaai wal-banaati wal-ikhwati wa akhwaati wal-

a'maami wal-ammaati wal-ah'waal wahaalati wal-ustaadh Abdul-hakeem Arwaasee wakaffatul mu'umineena wal-mu'uminaat. Rahamatullah ta'âlâ alayhim ajmaeen.

HAID ndi NIFAS
(Nsambo ndi Kutha kwa kubereka)

Masiku ochepetsetsa a nsambo ndi atatu ndipo akachulukitsa ndi khumi (10). Palibe masiku ochepa omwe ali nthawi ya kutha kubereka. Kutuluka kwa mwazi kukangosiya, ndi kofunikira kuchita ghusl, kuchita Namaz ndi kusala.

Kuchuluka kwa masiku odikira pambuyo pa kubereka ndi masiku makumi anayi. Ngati kutuluka kwa magazi kwa nsambo kusiya pasanate masiku atatu, (zimaganizidwa kuti si inali nsambo) ndipo mkazi wokhudzidwayo amachita qada[1] ya mapemphero a Namaz omwe sadachite chifukwa choganiza kuti akusamba. Sikufunika kuchita ghusl ya nsambo. Magazi akasiya kutuluka padytsa masiku atatu, (imeneyo ndi nsambo) ndipo nkofunika kuti mkaziyo achite ghusl ndikuchita namaz ya mu nthawi yomwe akuganiza kuti wamalizira nsambo. Masiku khumi akakwana, mkazi amachita ghusl ndikuchita namaz ya mu nthawi yomwe akuganiza kuti wamalizira nsambo. Izi adzachita posalabadira kuti magazi asiya kutuluka kapena ayi. Chimodzimodzi masiku makumi anayi akatha,pambuyo po bereka, eye amachita ghusl ndi kuchita namaz yake mosasamala kuti mwaziwo watha kapena ayi. Zotuluka za mtundu uliwonse pa masiku osamba kapena kutha kwa nthawi yobwreka ziyenera kuganiziridwa kuti ndi kuuka kwa magazi. Ngati magazi asiya kutuluka kwa tsiku kapena masiku awiri mkati mwa masiku khumi a nsambo kapena masiku makumi anayi pa kutha kwa kubereka, ndipo mkazi wachita ghusl ndi kusala kudya poganiza kuti magazi asiya, kenako magazi ndikuyambiranso mkati mwa nthawiyo, iye ayenera kuchita qada ya kusala komwe wachita kale ngati kuti sanazichite nkomwe. Ndipo adzachitanso ghusl magazi akasiya kutuluka.

Kutuluka kwa magazi kukasiya adat ya mkazi isanakwane (masiku omwe mkazi amatsirizira nsambo), koma patadutsa masiku atatu, ndiye kuti achita ghusl ndi kuchita namaz. Koma asagonane ndi

[1] Kuchita Qada ndi chinthu chopembedza cha Fardh chomwe chimachitidwa nthawi yake yochitika itatha.

mwamuna wake mpaka adat yake itatha. Lamulo lomweli limagwiranso ntchito mu nthawi ya kutha kobereka.

Ngati magazi atasiya kutuluka adat[1] yake itakwana, kaya pa tsiku lachikhumi kapena lisanakwane, nthawi yonseyo itengedwe kuti ndi thawi ya haid (nsambo). Koma ngati magazi sakusiya kutuluka pakutha pa masiku khumi, kutuluka magazi kuyambira pa tsiku la adat yake siyidzawerengedwa kuti ndi nsambo. Kotero adzaswali ma qada a masiku a pambuyo pa adat yake. Masiku 40 a pambuyo pobereka ali chimodzimodzi ndi masiku khumi a kusamba.

Pamene haid (nsambo) kapena nifas (nthawi ya pambuyo pobereka) ikutha mmawa wa Ramadan, iye asadye kapena kumwa, akhale ngati wasala tsiku limenelo.

Koma sikuti kudzakhala kusala kudya. Adzapanga qada ya tsiku limenelo kapena kuti adzayenera kumanga tsiku limodzi kumapeto kwa mwezi wodalitsika wa Ramadan. Ndipo ngati magazi ayamba kutuluka m'bandakucha, kaya awaona kumasana, mkaziyo adya ndi kumwa mobisa. Mkazi akaona kuti akutuluka mwazi, amayenera kusiya kuchita namaz ngakhale kusala kudya (kufunga). Ndipo magazi akasiya tsiku lachitatu lisanathe, adikire moleza mtima mpaka nthawi ya Namaz itatha, ndipo ngati magazi akutulukabe asachite namaz. Koma ngati magaziwo sakuonekanso, amachita udhu ndi kuchita namaz, ndipo ngati magazi ayambiranso kutuluka, amasiyanso kuchita Namaz. Kutaya magazi kukasiyanso, amadikilira mpaka nthawi ya Namaz itatsala pang'ono kutha ndipo amachita udhu ndi kuchita Namaz ngati magazi sakutulukanso. Apitiriza chomwecho mpaka tsiku lachitatu litatha, ndipo ghusl (kusamba) sikofunikanso. Udhu wokha ndi wokwanira. Kutuluka magazi kukasiya patatha tsiku lachitatu, mkaziyo adikire mpaka nthawi ya Namaz itayandikira nkuchita. Achite ghusl ndikuchita namaz yake ngati magaziwo sakuyambiranso kutuluka. Koma ngati atulukanso, amasiya kuchita namaz. Ngati zikupitilira kwa masiku khumi, iye adzachita ghusl ndi kuchita namaz yake ngakhale magazi akutulukabe. Lamuloli limagwiranso ntchito pa nkhani ya nifas (nthawi ya pambuyo pa kubereka). Koma ghusl idzakhala yofunikira nthawi iliyonse pomwe magazi asiya kutuluka, ngakhale atasiya tsiku loyamba. Mu Ramadan ngati magazi asiya

[1] Nthawi ya pakati pa tsiku lomwe magazi akuwoneka kuti ayamba ndi tsiku lomwe akuwoneka kuti akusiya imatchedwa adat. Masiku osachepera atatu ndi masiku osapitilira khumi malinga ndi Madhhab a Hanaf; tsiku limodzi ndi masiku khumi ndi asanu atatu malinga ndi Madhhab a Shafi'i ndi Hanbali.

kutuluka m'bandakucha, amaswali. Kutaya magazi kukayambiranso mu nthawi ya kushluk, (ya masana) kapena ku madzulo, kusala kwake sikukhla kusala. Choncho adzachita qada mwezi wa Ramadan ukatha.

Ngati wapita padera, zidzakhala ngati wabereka mwana wopanda chilema ngati tsitsi, pa kamwa kapena mphuno zake zitapangika. Ngati ziwalo zake sizinapangike, ndiye kuti sinkhani ya nifas (kubereka). Koma ngati magazi angatuluke kwa masiku atatu kapena kuposerapo, adzakhala ngati wachita nsambo. Koma siyidzakhala nkhani ya haid (nsambo) ngati kupita paderako kwachitika patatha masiku khumi ndi asanu kapena kuposerapo atatha nsambo. Ndipo magazi atsopanowo amatha masiku atatu asanathe, kapena ngati masiku khumi ndi asanu sanadutse atachita nsambo. Uku ndi kutuluka magazi chabe monga kamfuno. Ayenera kupanga Namaz. Ndipo ayenera kusala. Ghusl siyofinikira kwenikweni asanakagone ndi mwamuna wake.

[Katswiri wamkulu wa Chisilamu (Zeyn-ud-din) Muhammad Birgivi bin 'Ali “rahmatullâhi ’alaih” (928 [1521 A.D.], Balikasir – yemwe anamwalira ndi mliri mu 981 [1573], Birgi, Aydin, Turkey,) analemba bukhu lofunika kwambiri lotchedwa **Zuhr-ul-mutaahilin** momwe wafotokoza za nsambo wa amayi ndi nthawi ya pambuyo pa kubereka.

Bukuli lili mu chiyankhulo cha Chiarabu. Allama Shami Sayyid Muhammad Amin Ibni Abidin “rahima-hullâhu ta’âlâ” (1198 [1784 AD], Damascus - 1252 [1836], malo omwewo) anakulitsa bukhulo ndi kulitcha kuti **Menhel-ul-waridin**. Izi ndi zomwe zalembedwa mu **Menhel**-ul-waridin: Zanenedwa ndi akatswiri a Fiqh mogwirizana kuti ndi fardh kwa Msilamu aliyense, mwamuna kapena mkazi mofanana, kuphunzira (chiphunzitso cha Chisilamu chotchedwa) Ilmihal. Pa chifukwa chimenecho, akazi ndi amuna awo ayenera kuphunzira chiphunzitso chokhudza haid ndi nifas. Amuna aphunzitse akazi awo ngati akuzidziwa koma ngati sakuzidziwa, awalole kuphunzira kuchokera kwa akazi ena omwe akudziwa. Mkazi amene sakuloledwa ndi mamuna wake kukaphunzira ayenera kupita kukaphunzira popanda chilolezo cha mamuna wake.

Maphunzitso amenewa, omwe amakhudza akazi, zikuoneka kuti akuyiwalika, chifukwa palibe amuna a chipembedzo amene akudziwa za izi. Amuna achipembedzo amakono sanaphunzire mokwanira kuti angathe kulekanitsa mitundu ya magazi yotchedwa haid (kuchita nsambo), nifas (otuluka pambuyo pobereka), ndi istihada (kukakamira mu nsambo). Iwo alibe mabuku otambasula nkhani zimenezi. Ndipo omwe ali ndi mabuku okhala ndi kudziwa uku, sangathe kuwaŵerenga ndi kuwamvetsa. Ziphunzitso zimenezi ndi zovuta kumvetsa. Komano,

zinthu za chipembedzo monga nsambo, namaz, kuwerenga kapena kulakatula Qur’an al-kareem, kusala, I'tikaf, Hajj, kutha nsinkhu, kukwatira, kusudzula ndi kusudzulidwa, iddat ya mkazi (Nthawi yodikira mkazi amuna ake akamwalira kapena akamudzudzula), istibra, ndi zina zotero, zimafunika kuphunzira zambiri zokhudzana ndi mitundu ya kutaya magazi. Zinanditengera theka la moyo wanga kuti ndimvetse bwino ziphunzitso zimenezi. Ndiyesera kufotokoza mwachidule komanso momveka bwino zomwe ndaphunzira kuti zithandize alongo anga a Chisilamu:

Haid ndi magazi omwe amayamba kutuluka kumalo obisika a mtsikana wathanzi (osachepera) zaka zongopitilira pang'ono zisanu ndi zitatu (8) za kubadwa, kapena kuchokera kwa mzimayi atamaliza nthawi yake ya chiyero chake yobwera motsatizana ndi mphindi yomaliza ya nsambo wake wam'mbuyo. Ndipo zimapitilira kwa masiku osachepera atatu. Kutuluka kwa magazi kumeneku kumatchedwanso kuti ndi kutuluka magazi kwa sahih. Nthawi yomwe magazi asakutuluka nyengo yokwana masiku khumi ndi asanu kapena kuposerapo, potsatira adat ya munthu (nthawi ya pakati pa minsambo iwiri), nthawi ya chiyero imeneyi imatchedwa kuti ndi chiyero cha sahih. Ngati pali masiku omwe magazi atuluka kwa fasid pasanadutse kapena pambuyo pa masiku khumi ndi asanu kapena kupitilira apo kapena pakati pa nyengo ziwiri za chiyero cha sahih, masiku onsewa (omwe asokonezeka ndi masiku a kutuluka kwa magazi kwa fasid) amatchedwa **Chiyero cha hukmi** kapena **fasid wa chiyero.**

Nthawi yomwe magazi saoneka koma yosapitilira masiku khumi ndi asanu imatchedwa chiyero cha fasid. Chiyero cha Sahih ndi chiyero cha hukmi zimatchedwa ziyero zokwanira. Magazi omwe amawoneka nthawi isanakwane ndi itatha nthawi yoyera koma yomwe imapitilira kwa masiku osachepera atatu ndi nyengo ziwiri zosiyana za haid.

Mtundu wa magazi uliwonse kupatula oyera koma kuphatikizapo mtundu wamtambo, ndi magazi a nsambo.

Mtsikana akayamba kusamba amakhala **baligha**, (ndiko kuti watha msinkhu.) Kapena kuti wafika pa uzimayi. Chiwerengero cha masiku pakati pa nthawi yomwe magazi ayamba kutuluka ndi tsiku limene magazi asiya ndi nthawi ya **adat.** Nthawi ya adat ndi malire masiku khumi. Akachepetsetsa ndi masiku atatu. M'Madhhab a Shafi'i ndi Hanbali amati ndi masiku khumi ndi asanu (akachuluka) ndi tsiku limodzi akachepa.

Haid sizitanthauza kutuluka kwa magazi kosalekeza. Ngati kutuluka kwa magazi kwayamba ndi kusiya koma ndikuyambira patapita tsiku

limodzi kapena awiri, nthawi ya chiyero yomwe yachitika pa masiku apakatipo imawerengeredwa ku nthawi yotuluka magazi mosalekeza. Izi zili chonchi, malinga ndi kumvana kwa akatswiri a Chisilamu. Ngati chiyerocho chipitilira kwa masiku atatu kapena kupitilira apo ndikutha tsiku la khumi la Haid lisanafike, ziyenera kuganiziridwa kuti magazi amapitilirabe kwa masiku khumi. Izi zili choncho malinga ndi malipoti omwe Imam Muhammad “rahima-hullâhu ta’âlâ” anapereka kuchokera kwa Imam Azam Abu Hanifa “rahima-hullâhu ta’âlâ”. Palinso lipoti lina la ukatswiri loperekedwa ndi Imam Muhammad.

Malinga ndi kunena kwa Imam Abu Yusuf “rahima-hullâhu ta’âlâ”, masiku onse achiyero amene atha tsiku lakhumi ndi chisanu lisanakwane, adzaonjezeredwa ku nthawi ngati kuti magazi amatuluka mosalekeza. Tiyerekeze mtsikana akaona kutuluka kwa magazi tsiku limodzi ndikutsatira masiku khumi ndi anayi oyera, ndikudzatuluka magazi kwa tsiku limodzinso, masiku khumi oyambilirawo ndiwo amapanga adat yake malinga ndi Imam Abu Yusuf. Kapena mzimayi kutuluka magazi tsiku limodzi, kenako masiku khumi akuyeretsedwa motsatira tsiku limodzi lotuluka magazi, chiwerengero cha masiku olingana ndi adat yake ndiwo masiku a nsambo ake; koma masiku onse otsatira pambuyo pake adzakhala masiku a istihada (Nsambo yosalekeza). Kapena mkazi kutuluka magazi kwa masiku atatu, kenako ndi kukhala chiyero kwa masiku asanu ndi kudzatulukanso tsiku limodzi, masiku onse asanu ndi anayi amakhala a nsambo. Malinga ndi riwayah (lipoti la katswiri) ya Imam Muhammad's “rahima-hullâhu ta’âlâ”, masiku asanu ndi anayi okha a mkazi woyambilirayo ndi omwe angakhale a nsambo (haid).

Malinga ndi riwayat yachiwiri ya Imam Muhammad, masiku atatu okha oyambilira a mkazi wotsirizayo ndi omwe ali a nsambo, ndipo masiku enawo si masiku a nsambo. Kumasulira kuchokera m'bukhu la **Multaqa,**[1] mu bukhu lathu lino, talemba zonse zotsatirazi potsatira riwayat yoyamba ya Imam Muhammad. Tsiku limodzi likuyimira ndendende maora makhumi awiri ndi anayi (24). Ndi mustahab (zolimbikitsidwa), kwa akazi osakwatiwa (anamwali) pa nthawi ya nsambo yokha, komanso kwa akazi okwatiwa nthawi zonse, kuyika nsalu kapena thonje lotchedwa kursuf (padi, liner wa panti) pakhomo pa malo awo obisika, ndi kugwiritsa ntchito mafuta onunkhira. Ndi makruh (zonyansa) kwa iwo kulowetsa kursuf yonse ku maliseche.

[1] Lolembedwa ndi Ibrahim bin Muhammad Halabi “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih” (866, Aleppo – 956 [1549 AD], Istanbul.

Mtsikana amene akuona madontho a magazi pa kursuf tsiku lililonse kwa miyezi yotsatizana ayenera kuwerengeredwa kuti amakhala pa nsambo kwa masiku khumi oyambilira okha ndipo kuti masiku enawo ndi istihada kwa masiku makumi awiri otsatirawo m'mwezi uliwonse. Lamuloli ligwire ntchito mpaka kutaya magazi kosalekeza kumeneku kutatha. Kutaya magazi kosalekeza kumeneku kumatchedwa **istimrar.** Mtsikana akawona magazi kwa masiku atatu mosalekeza kenako ndikusawaona kwa tsiku limodzi kenako nkuwaonanso kwa tsiku limodzi kenako osawaona masiku awiri mosadukiza kenako nkuwaonanso kwa tsiku limodzi kenako osawaona kwa tsiku limodzi kenako ndikuwaonanso kwa tsiku limodzi, masiku onse khumi ndi a nsambo. Ngati aona magazi tsiku limodzi koma osawaona mawa lake, ndipo ngati izi zipitilira kwa masiku khumi pa mwezi uliwonse, ndiye kuti asiya namaz ndi kusala chakudya tsiku lina lililonse lomwe akuwona magazi, ndipo azichita ghusl ndikuchita Namaz zake za pa tsiku pa tsiku lirilonse lomwe magazi sakutuluka [Mesail-i-sharh-i-wikaya].[1] Kutaya magazi kwa nthawi yochepera masiku atatu, omwe ali maora makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri (72), kaya kucheperako ndi mphindi zisanu sikutengedwa ngati nsambo. Kwa msungwana yemwe wakula kumene msinkhu, yemwe amadwala masiku khumi ndipo akupitilira kwa masiku oposanso khumi naye kudwalako sikuzatengedwa kuti ndi nsambo. Kapena kwa mkazi yemwe anakula msinkhu kale, akutuluka magazi kupitirira adat yake komanso kuphola masiku khumi, naye sazatengedwa ngati nsambo. Chimodzimodzi kutuluka magazi kwa mzimayi woyembekezera kapena aisa [wachikulire] kapena namwali wochepera zaka zisanu ndi zinayi, nawo sangawerengeredwe kuti ndi nsambo. Zoterezi zimatchedwa **istihada** (kukakamira ku nsambo), kapena magazi a fasid. Mkazi amakhala **aisa** akakwana zaka pafupifupi makumi asanu ndi zisanu (55). Mkazi yemwe adat yake ndi masiku asanu akatuluka magazi pamene theka la dzuwa latuluka ndipo magazi ake akutha pamene magawo awiri pa atatu a dzuwa limatuluka m'mawa wa tsiku la khumi ndi limodzi, kutuluka kwa magazi opitilira adat yake ya masiku asanu kudzawerengeredwa kuti ndi istihada (kukakamira ku nsambo).

Popeza kutuluka magazi kwake kwadutsa muyezo wovomerezeka wa masiku khumi, kuonjezera usiku khumi ndi gawo limodzi mwa magawo asanu ndi limodzi a kutuluka kwa dzuwa. Akatha masiku

[1] Bukhu limenelo, m'chiyankhulo cha Farisi, lolembedwa ndi Abd-ul-Haqq Sujadil Serhendi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih".

khumi, achite ghusl ndi kuchita qada za Namazi zomwe sadachite m'masiku otsatira adat yake.

Mkazi amene ali mu nthawi ya istihada ndi munthu amene ali ndi udhr, monga amene akudwala matenda otupa m'mphuno kapena kamfuno wosalekeza. Ayenera kuchita namaz ndi kusala kudya, ndipo waty (kugonana) nkololedwa kwa iye.

Malinga ndi qawl ya Imam Muhammad, mtsikana yemwe kuyamba kumene kutuluka magazi koyamba m'moyo wake, ndipo ngati kukuchitika kwa tsiku limodzi ndi kupuma kwa masiku asanu ndi atatu ndikubweleranso pa tsiku lakhumi, masiku khumi onsewo amawerengedwa kuti ndi a nsambo. Koma, ngati watulutsa magazi kwa tsiku limodzi ndi kupuma kwa masiku asanu ndi anayi otsatirawo ndi kubweleranso tsiku la khumi ndi limodzi, izi zidzawerengedwa kuti palibe nsambo. Kutuluka magazi kwa masiku awiriwo ndi istihada. Monga zanenedwa kale, masiku a chiyero pambuyo pa kutuluka kwa magazi komwe kumawonedwa pambuyo patsiku lakhumi sawerengedwa ngati kusamba. Akaona magazi pa tsiku lakhumi ndi lakhumi ndi limodzi, masiku oyeretsedwa pakati pawo adzawerengedwanso ngati kusamba, ndipo masiku khumi oyambilira adzakhala a nsambo ndipo tsiku lakhumi ndi chimodzi lidzakhala istihada.

Istihada (Nsambo yokakamira) ndi chizindikiro cha matenda. Kutuluka magazi kwa nthawi yaitali kwambiri kungakhale koopsa. Ndi pofunika kukaonana ndi dokotala. Red gum wotchedwa 'dragon's blood' chimaletsa kutuluka kwa magazi ngati chitaumbidwa mu timipira tating'ono ndi kumeza ndi madzi kawiri tsiku, gramu imodzi m'mawa ndi ina madzulo

Mlingo oyenelera kumwa tsiku usapitilire magalamu asanu. Nthawi ya nsambo ndi ya chiyero ya mkazi ndi masiku ofanana m'mwezi uliwonse. Apatu tikati mwezi umodzi, ndi nthawi ya pakati pa chiyambi cha haid imodzi ndi inzake. Mkazi aliyense ayenera kuphunzira pa mtima chiwerengero cha masiku ndi maola amene amasamba ndi masiku ake ndi maola omwe amakala mchiyero. Adziwe adat yake popeza kuti adat ya mkazi siyisintha kwa zaka zambiri. Ngati zisintha, adzayenera kuloweza masiku ake atsopano a haid ndi chiyero.

Bukhu lotchedwa **Menhel** (ul-waridin) likupereka nkhani yotsatirayi pakusintha kwa adat: Ngati mkazi akusamba molingana ndi nthawi za masiku ake akale, ziyenera kuganiziridwa kuti adat yake siinasinthe. Ngati siikutsatidwa, ndiye kuti adat yake yasintha, ndipo mitundu ya kusinthaku ikufotokozedwa m'masamba otsatirawa.

Ngati yasintha kamodzi kokha, ndiye kuti adat imavomerezedwa kuti yasintha. Lamuloli likutsimikizikanso ndi fatwa. Ngati mkazi amene amadwala masiku asanu aona kutuluka kwa magazi kwa masiku asanu ndi limodzi pambuyo pa kuyeretsedwa kwa sahih, masiku asanu ndi limodzi amenewa adzakhala haid yake yatsopano, adat yatsopano. Masiku achiyero adzasinthanso molingana ndi kusintha kamodzi komwe kwachitika. Zikasintha choncho, adat nayo imasintha. Tiyerekeze kuti adat ya mkazi ndi masiku asanu akutuluka magazi otsatiridwa ndi masiku makumi awiri ndi asanu akuyera; ngati adat yake yatsopanoyo ikhala masiku atatu akukha magazi motsatizana ndi masiku makumi awiri ndi asanu akuyeretsedwa kapena masiku asanu otuluka magazi kutsatiridwa ndi masiku makumi awiri ndi atatu akuyeretsedwa, ndiye kuti masiku otuluka magazi kapena oyeretsedwa, motsatana, adzasintha chiwerengero. Momwemonso, ngati kutuluka magazi kupyola masiku khumi, kotero kuti kutuluka magazi kwa fasid kuchitike ndipo masiku atatu kapena kuposerapo akutuluka magaziwo agwirizana ndi masiku a adat yake yam'mbuyo ndi masiku otsala a adat yake yam'mbuyo a kuyeretsedwa kwatsopano, masiku ogwirizana ndi masiku ake (am'mbuyo) a adat ndi adat yake yatsopano. Apa ndiye kuti adat yake yasintha tsopano.

Ngati adat yake ndi masiku asanu, ndipo kutuluka kwa magazi kutayamba masiku asanu ndi awiri (7) masiku ake akuyeretsedwa asanathe, ndipo magaziwo apitilira kwa masiku khumi ndi limodzi, ndiye kuti kutuluka kwa magaziwo ndi kwa fasid chifukwa chakuti kwadutsa masiku khumi. Masiku opitilira atatu akutuluka kwa magazi, kutanthauza kuti akwana masiku anayi, ali mkati mwa 'adat yake yam'mbuyo, ndipo tsiku limodzi la 'adat yake ya m'mbuyomu limalowa m'chiyero chatsopano cha sahih. Nthawi yake ya 'adat tsopano idzakhala masiku anayi, ngakhale kuti nthawi yomwe zimachitika siinasinthe. Tiyeni tifotokoze momveka bwino za kusintha kwa mtundu umenewu mu 'adat:

Ngati masiku atsopano otaya magazi omwe ali m'chiwerengero chosiyana ndi omwe adawatsogolera kupitilira masiku khumi ndipo masiku atatu kapena kuposerapo osachitika m'masikuwo ya 'adat yake yapitayo, nthawi yomwe 'adat imachitika imasintha. Apa sipamakhala kusintha kwa chiwerengero cha masiku (a ’adat) popeza kuwerengera kumayamba tsiku limene magazi aoneka. Ngati mkazi amene 'adat yake ndi masiku asanu saona kutuluka kwa magazi m'masiku asanuwa m'mwezi wotsatira, kapena ngati saona magazi akutuluka m'masiku atatu oyambilira, ndipo kenako nkuona magazi kwa masiku khumi ndi

limodzi, ndiye kuti kusamba kwake kuli koyenera masiku asanu, kuyambira tsiku limene magazi anaonekera koyamba; komabe nthawi yake yasintha. Ngati kutuluka kwa magazi kwa tsopanoko kukuchitika m'masiku a adat yake yapitayo, masiku atatu kapena oposerawo ndi amene ali a nsambo, masiku otsalawo ndi istihada (kukakamira ku nsambo).

Ngati kutuluka kwa magazi kuyamba masiku asanu (5) mofulumirirapo poyerekeza ndi mmene adat yake inaliri m'mbuyomu, kenako ndi kusawaona magazi m'masiku omwe m'mbuyomu amakhala pa nsambo kenako ndi kudzaona kutuluka kwa magazi kwa tsiku limodzi pambuyo pa masiku a adat yake ya m'mbuyomo, masiku asanu a chiyero apakatiwo ndi nsambo ndipo adat yake siinasinthe. Izi zili chonchi malinga ndi Imam Abu Yusuf. Ngati aona magazi m'masiku atatu omalizira a adat yake yam'buyo ndiponso kwa masiku ena asanu ndi atatu motsatizana, masiku atatu oyambilira ndi nsambo, ndipo chiwerengero chasintha. Ngati masiku a magazi owonjezera ndi ocheperako kuti sakukupyola masiku khumi ndi kutsatira chiyero cha sahih, masiku atatuwo kuphatikiza masiku ochepera asanu ndi atatu ndi nsambo. Ngati chiyero chotsatira chili chiyero cha fasid, ndiye kuti adat yake siyingasinthike. Ngati adat yake ili ya masiku asanu, koma ndi kuona magazi kwa masiku asanu ndi limodzi, kenako ndi kukhala woyera kwa masiku khumi ndi anayi, ndipo ndi kuoneka magazi kwa tsiku limodzi, ndiye kuti adat yake sinasinthe. Tiyeni tipereke zitsanzo khumi ndi chimodzi pogwiritsa ntchito mkazi wongoyerekeza yemwe adat yake imakhala ndi masiku asanu a haid ndi masiku makumi asanu ndi asanu achiyero kuti tisindike mwatsatanetsatane pa zomwe zanenedwa kale:

Ngati mkaziyo adutsa mu nyengo ya nsambo kwa masiku asanu ndi masiku khumi ndi asanu a chiyero kenako masiku khumi ndi limodzi a magazi, kumachita kuti magazi sakutuluka ngati momwe zimakhalira mu nthawi ya adat yake m'mbuyomu, zomwe zikanachitika patatha masiku makumi asanu ndi asanu (ndiye kutha kwa adat yake ndi masiku asanu). Choncho, nthawi ya adat yasintha koma chiwerengero cha masiku ake sichinasinthe. Masiku asanu oyambilira a m'masiku khumi ndi limodzi akumapetowo ndi nsambo.

2- Mkazi akatuluka magazi masiku asanu motsatizana mosatizana ndi masiku makumi anayi ndi asanu ndi limodzi a chiyero ndi masiku khumi ndi limodzi otuluka kwa magazi, pamenepo masiku awiri omalizira a masiku khumi ndi limodzi omalizirawo amakhala m'nyengo ya adat. Koma popeza ndi masiku osakwana atatu, chiwerengero cha

masiku a adat sichisintha ngakhale kuti nthawi yake inasintha. Ndiye, masiku asanu oyambilira mwa masiku khumi ndi limodziwo ndi nsambo.

3- Ngati akumana ndi masiku asanu akusamba ndi masiku makumi anayi ndi asanu ndi atatu (48) a chiyero, kenako masiku khumi ndi awiri (12) okutuluka magazi, asanu mwa masiku khumi ndi awiriwo omwe ndi masiku makumi asanu ndi asanu a chiyero, ndipo masiku asanu ndi osamba. Kotero, palibe kusintha komwe kwachitika.

4- Akatuluka magazi kwa masiku asanu ndi masiku makumi asanu ndi anayi (54) a chiyero, ndi tsiku limodzi lakukha kwa magazi, ndi masiku khumi ndi anayi (14) a chiyero, kenako tsiku limodzi lakukha kwa magazi, tsiku limodzi la pakatilo, (tsiku loyambilira loyambalo), ndi tsiku lomaliza la chiyero chake cha nthawi zonse. Popeza kuti masiku khumi ndi anayi ndi chiyero cha naqis (chopunguka), kapena tinene kuti chifukwa chakuti masiku asanuwo ndi ochepera pa masiku aukhondo wovomerezeka, atengedwa kuti ndi masiku akutuluka magazi, ndipo asanu oyambawo ndi a nsambo. Nthawi ya adat ndi chiwerengero cha masiku ake sizinasinthe.

5- Masiku asanu otuluka magazi otsatizidwa ndi masiku makumi asanu ndi mphambu zisanu ndi awiri (57) a chiyero otsatiridwa ndi masiku atatu akukha kwa magazi motsatizana ndi masiku khumi ndi anayi achiyero otsatiridwa ndi tsiku limodzi lotuluka magazi; masiku atatu akutuluka magaziwo amakhala mkati mwa nthawi ya adat. Masiku khumi ndi anayi otsatirawo awerengedwe ngati masiku akukha kwa mwazi. Koma popeza kuti chiwerengero cha masiku chaposa masiku khumi ndi limodzi, adat yasintha m'chiwerengero chake cha masiku okha.

6- Ngati ndi masiku asanu a magazi ndi masiku makumi asanu ndi asanu (55) a chiyero, kenako masiku asanu ndi anayi a magazi otsatiridwa ndi chiyero cha sahih zaonekera, masiku asanu ndi anayi omaliza a magaziwo ndi nsambo. Chiwerengero cha masiku a adat ndi chomwe chasintha. Pali masiku oposa atatu monse, panthawi ya adat ndi pambuyo pake.

7- Titenge masiku asanu a magazi ndi kutsatiridwa ndi masiku makumi asanu a chiyero ndi masiku khumi a magazi; ndiye kuti masiku khumiwo ndi a nsambo. Masiku a chiyero asintha kukhala masiku makumi asanu. Masiku otuluka magazi ali m'nthawi ya adat, ndipo chiwerengero chawo chirinso chofanana.

8- Pakakhala masiku asanu a magazi, ndi masiku makumi asanu ndi anayi a chiyero, ndi masiku asanu ndi atatu akutulukanso magazi;

masiku asanu ndi atatuwo ndi a nsambo, ndipo masiku oposera atatu mwa iwo ali mu adat. Chiwerengero cha masiku osamba ndi oyera chisintha ndi tsiku limodzi.

9- Titenge masiku asanu akukha magazi ndi masiku makumi asanu a chiyero ndi masiku asanu ndi awiri akukhanso magazi; masiku asanu ndi awiriwo ndi a nsambo, masiku ochuluka okwanira ndi oyenerera ali pasanafike adat ndipo masiku ochepera atatu ali mu chiwerengero chiyenera. Kotero, nsambo wasintha mu nthawi yake ndi chiwerengero cha masiku, pamene masiku a chiyero angosintha chiwerengero.

10- Titenge masiku asanu akutuluka magazi, ndi masiku makumi asanu ndi asanu ndi atatu (58) a chiyero, ndi masiku atatu akukhanso magazi; masiku atatuwo adzakhala a nsambo, masiku awiri mwa amenewo adzakhala m'nthawi ya adat ndipo tsiku limodzi pambuyo pake. Apa adat ya nsambo yasintha mu nthawi yake komanso chiwerengero cha masiku ake, ndipo chiyero chasintha m'chiwerengero chokha cha masiku ake.

11- Timalize ndi kufanizira masiku asanu akutuluka magazi, ndi masiku makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zinayi (64) a chiyero, ndi masiku asanu ndi awiri (7) kapena masiku khumi ndi limodzi (11) akukha magazi; mu nkhani yoyamba, masiku asanu ndi awiri wo ndi nsambo, pomwe kusintha kwachitika mu adat ndi mu nthawi. Mu nkhani yotsirizayi, masiku asanu oyambilira mwa masiku khumi ndi limodzi ndi nsambo, masiku asanu ndi limodzi otsalawo ndi istihada. Adat yasintha mu nthawi yake yokha. Popeza kutuluka magazi kukupitilira kwa masiku oposa khumi, chiwerengerocho sichimasintha. Chiyero chimasintha mu chiwerengero cha masiku ake.

Zinanenedwa motere ndi Imam Fakhr-ud-din 'Uthman Zeyla'i "rahima-hullâhu ta'âlâ" (d. 743 [1343 A.D.], Egypt), m'buku lake la **Tebyin-ul-haqaiq**, Komanso ndi Ahmad bin Muhammad Shelbi "rahima-hullâhu ta'âlâ" (d. 1031 [1621 AD], Egypt), popereka ndemanga pa bukhulo: "Ngati magazi atatuluka patatsala tsiku limodzi la adat yake ndi masiku khumi a chiyero kenako magazi ndi kutuluka tsiku limodzi, malinga ndi Imam Abu Yusuf "rahima-hullâhu ta'âlâ", nsambo yake, imayamba ndi masiku khumi omwe sanawone kutuluka kwa magazi ndipo imapitilira nthawi yonse ya adat yake. Tsiku loyamba ndi ndi lotsiriza nsambo yake yatsopano ndi opanda magazi. Pakuti, magazi aoneka adat isanadze ndi pambuyo pa tsiku la khumi, zomwe zikutanthauza kuti chiyero cha fasid pakati pake chiwerengedwa ngati masiku akukha magazi. Malinga ndi kunena kwa

Imam Muhammad “rahima-hullâhu ta’âlâ”, nthawi yonseyi ndi si yosasamba. Tiyerekeze kuti adat ya mkazi ndi masiku asanu otuluka magazi, kenako ndi masiku makumi awiri ndi asanu (25) a chiyero:

1- Ngati magazi atuluka tsiku limodzi mufulumirira, ndi tsiku limodzi la chiyero pambuyo pa tsiku limodzi lotuluka magazi, ndipo pambuyo pake kutuluka magazi kuyambiranso ndikupitilira ndi njira yotchedwa 'istimrar' (kupitilira mosalekeza) komwe kukupitilira tsiku la khumi, masiku asanuwo, omwe ali adat yake ndi nsambo, malingana ndi Imam Abu Yusuf. Masiku oyambilira ndi masiku otsatira pambuyo pake a kutuluka kwa magazi adzakhala (istihada). Malinga ndi Imam Muhammad, atatu mwa masiku akukha magazi, mwachitsanzo, omwe amagwirizana ndi adat yake, ndi nsambo. Masiku atatu amenewo ndi tsiku lachiwiri, lachitatu ndi lachinayi la adat yake. Poti sanatuluke magazi tsiku loyamba la adat yake. Tsiku lachisanu mwa masiku omwe anatuluka magazi, ali kunja kwa adat yake.

2- Ngati aona magazi pa tsiku loyamba la adat yake, ndipo pambuyo pake tsiku limodzi la chiyero lomwe likutsatiridwa ndi kutuluka magazi kosalekeza kotchedwa 'istimrar' komwe kukupitirira tsiku la chikhumi; masiku asanu ngati ali mu adat yke adzakhala nsambo. Izi zanenera movomerezana ndi akatswiri a Chisilamu. Pakuti, tsiku loyamba ndi tsiku lotsiriza ndi a magazi.”

3- Ngati aona magazi kwa masiku atatu mu adat yake, ndipo pambuyo pake chiyero kwa masiku awiri ena, kenako ndi istimrar yomwe ikupitilira tsiku la khumi; apa ndiye kuti masiku asanu a adat yake ndi nsambo, malinga ndi Imam Abu Yusuf. Koma malinga ndi Imam Muhammad, masiku atatu oyambilira a dat yake ndi nsambo. Pakuti, mu ijtihad (matambasulidwe) a Imam Muhammad, masiku oyamba ndi omaliza a nsambo ayenera kukhala amagazi.

M’mabuku a **Bahr** ndi **Durr-ulmunteqa** zanenedwa motere: “Ngati kutuluka kwa magazi kupyola nthawi ya adat ndi kusiya masiku khumi asanathe ndipo sakunabwelerenso m’masiku khumi ndi asanu otsatira, ndiye kuti kutuluka kwa magazi m’masiku opitilirawo ndi nsambo. Izi zanenedwa ndi akatswili a Chisilamu mogwirizana. Zikatero, masiku a adat adzakhala kuti asintha.

Ngati magazi atuluka ngakhale kamodzi kokha usiku kapena masana m’masiku khumi ndi asanu, masiku opyola adat yake sadzakhala nsambo; adzakhala kutuluka kwa magazi kwa istihada. Ndipo masiku amenewo akadziwika kuti masiku okakamira ku nsambo, amachita qada Namazi zomwe sadachite m’masiku amenewo.” Ndi mustahab kwa iye kudikira mpaka kutha kwa nthawi

ya Namaz ya nthawi yomwe magazi asiya kutuluka, ngati kuthako kwachitika pambuyo poti adat yatha ndipo pasanathe masiku khumi. Ndiye achite ghusl ndikuchita Namaz nthawi imeneyo. Waty (kugonana) ndi kololedwa pambuyo pake. Ngati ataphonya ghusl ndi Namaz pamene akudikira, ndiye kuti nthawi ya Namaz ikadzatha, waty (kugonana) popanda kuchita ghusl ndi kololedwa.

Pamene namwali akuona kutuluka kwa mwazi ake kwa nthawi yoyamba m'moyo wake komanso komanso mkazi yemwe akuwona kutuluka kwa magazi ake patatha masiku khumi ndi asanu pambuyo pa kutha kwa adat yake, onse mwa awiriwa ngati kutuluka kwa magaziwo kusiya pasanathe masiku atatu, awiriwa adzayenera kudikira mpaka itatsala pang'ono kutha nthawi ya Swala ya nthawi yomwe kukha magazi kwalekeka. Kenako achita udhu popanda kuchita ghusl, ndikuchita namaz ya nthawiyo ndi kuchita qada Namazi zomwe sadachite pa nthawi yotaya magazi yomwe idapitilira masiku atatu. Kutaya magazi kukayambiranso atachita namaz, asapitilize kuchitanso namaz. Ikasiyanso, amachitanso wudhu chakumapeto kwa nthawi ya Swalah ndikuchita namaz ya nthawiyo ndi kuchita qada ma namaz omwe aphonya, ngati alipo. Amapitirizabe kuchita zimenezi mpaka kutha masiku atatu. Koma, waty (kugonana) si halal ngakhale ghusl itachitika.

Ngati, mu zitsanzozi ziwirizo, kutuluka kwa magazi kukupitilira masiku atatu koma nkuleka ndi kusiya adat isanathe, waty (kugonana) sikukhala halal mpaka nthawi ya adat itatha ngakhale atachita ghusl. Koma ngati saona banga la magazi mpaka ku mapeto kwa nthawi ya swala, achita ghusl ndikuchita namaz imeneyo. Sayenera kuchita qada namaz zomwe sadachite pa nthawiyo. Iye asala kudya. Ngati magazi satuluka kwa masiku khumi ndi asanu (15) pambuyo pa tsiku lomwe magazi adasiya, tsiku lomwe analeka ndilo mapeto a adat yake yatsopano. Koma magazi akabweleranso, amasiya namaz. Koma kusala kumene anachita, adzakuchita Qada pakutha pa Ramadan. Kukha kwa magazi kukasiya, achitenso ghusl chakumapeto kwa nthawi yopemphera ndi kuchita namaz. Asale kudya. Adzakhala akupitiriza kuchita chimodzimodzi mpaka patapita masiku khumi.

Pakatha tsiku khumi amachitanso namaz popanda kuchita ghusl ngakhale ataona kutuluka kwa magazi, ndipo waty (kugonana) asanachite ghusl ndi halal. Koma ndi mustahab kuchita ghusl asanachity waty. Kutuluka magazi kukaleka kusanache, ndipo ngati pali nthawi yokwanira kuchita ghusl ndi kuvala koma osanena kuti: "Allahu akbar," kusanache, amasala kusala kwa tsiku loyamba. Koma

sakuyenera kuchita qada ya Swalah ya usiku wa dzulo lake. Ngati pali nthawi yokwanira kunena takbir “Allahu akbar,” adzayenera kupanga qada ya Swalah ya usiku. Ngati Nsambo iyamba iftar isanakwane, shar’i, kulowa kwa dzuwa, nthawi yomasula kusala, amakhala kuti wamasula kusala kwake nthawi yomweyo. Adzachita qada yakusala kwa tsiku limenelo pambuyo pakutha kwa mwezi wa Ramadan. Nsambo ukayamba pa nthawi ya namaz, namaz yake imaonongeka. Akamaliza nsambo yake achite ghusl. Sayenera kuchita qada ngati idali namaz ya fardh. Koma ngati inali namaz ya nafila (zowonjezera), atha kuchita qada yake. M’mawamawa podzuka mkazi akaona magazi pa kansalu kake kodzisamalira (kursuf), nsambo yake yayamba nthawi yomwe waona magazi. Mkazi akawona kuti kansalu kake kodzisamalira ndi koyera akadzuka, ndiye kuti nsambo yake yatha iye ali m'tulo. M’njira zonsezi ndi fardh kuchita namaz ya usiku wa dzulo lake. Poti namaz kuti ikhale fardh kumafunika kukhala waukhondo, osakhala mu nyengo ya nsambo mpaka mphindi yotsiriza ya nthawi ya namazyo. Mkazi amene waona kuti ali nsambo yayamba asanapemphere Namaz ya nthawiyo, sayenera kuchita qada ya namaz imeneyo.

Payenera kukhala nthawi ya **chiyero** chenicheni pakati pa nthawi ziwiri za nsambo. Ngati nthawi ya chiyero imeneyi ndi yomwe imatchedwa **chiyero cha sahih**, ndiye kuti kutuluka kwa magazi chiyero chisanayambe ndi pomwe chiyeri chatha ndi ma haid (nsambo) ziwiri zosiyana, malinga ndi kugwirizana kwa akatswiri a Chisilamu. Masiku a chiyero m'kati mwa masiku otuluka magazi m'masiku khumi onse a Nsambo amavomerezedwa kukhala nsambo, pomwe masiku a istihada pambuyo pa masiku khumi amavomerezedwa kukhala masiku a chiyero. Namwali akatuluka magazi kwa masiku atatu, kenako masiku khumi ndi asanu osatuluka, kenako tsiku limodzi lotuluka magazi, kenako tsiku limodzi losatuluka, kenako ndi masiku atatu akukha magazi; masiku atatu oyamba ndi omaliza omwe amawona magaziwo ndi nthawi ziwiri zosiyana za nsambo. Popeza adat yake idzakhala ya masiku atatu, Nsambo yake yachiwiri siyingayambe ndi tsiku limodzi lokha la magazi pakati pake. Tsiku limodzi lotuluka magazilo limachititsa chiyero chake m’mbuyo kukhala cha fasid.

Mola Husraw “rahima-hullâhu ta’âlâ” (yemwe anamwalira mu 885 [1480 AD]) akuti ananena motere mu **Ghurer** popereka ndemanga ya Shernblali kwa: "Ngati namwali akutuluka magazi tsiku limodzi (1) ndikutsatizana ndi masiku khumi ndi anayi (14) a chiyero

ndikulumikizanso ndi tsiku limodzi (1) lotuluka magazi ndikudzatsatizananso ndi masiku asanu ndi atatu (8) a chiyero, kutsatiridwa ndi tsiku limodzi (1) la magazi ndi kutsatira masiku asanu ndi awiri (7) a chiyero ndi kutsatira masiku awiri (2) akukha magazi ndi kutsatira masiku atatu (3) a chiyero ndi kutsatira tsiku limodzi (1) la magazi lotsatiridwa ndi masiku atatu (3) a chiyero ndi kutsatira tsiku limodzi (1) la magazi ndi kutsatira masiku awiri (2) a chiyero ndikutsatira limodzi la magazi; mwa masiku makumi anayi ndi asanu amenewa, masiku khumi okha otsatira masiku khumi ndi anayi ndiwo ali a nsambo. Masiku enawo ndi istihada, malinga ndi kunena kwa Imam Muhammad “rahima-hullâhu ta’âlâ”.” Poti nsambo yatsopano siyiyamba pajutha pa masiku khumi amenewa, popeza palibe chiyero chokwanira. Masiku a ukhondo otsatira pambuyo pake sakhala ovomerezeka poti ndi masiku omwe magazi amatuluka mosalekeza, chifukwa sali mkati mwa nyengo ya nsambo. "Malinga ndi Imam Abu Yusuf “rahima-hullâhu ta’âlâ”, masiku khumi oyambirirawo ndi masiku khumi achinayiwo omwe ali ndi chiyero kumbali zao zonse ndi nsambo.” Poti molingana ndi Imam Abu Yusuf, masiku a chiyero omwe adawatsatira ndi masiku omwe kukha kwa magazi kumavomerezeka kuti kunachitika mosalekeza. Potengera nkhani yoyambayo, pambuyo pa masiku khumi a nsambo, masiku makumi awiri ndi masiku a chiyero ndipo masiku khumi otsirizawo, [masiku khumi achinayi,] ndi nsambo.

Ngati magazi apitilira kutuluka kwa masiku khumi ndi asanu popanda masiku a chiyero pakali pawo, kuchucha magazi kutchedwa istimrar, kuwerengetsa kumachokera pa adat yake. Ndiye kuti kuyambira ikangotha adat yake, nthawi ya chiyero ifanana ndi chiwerengero cha masiku a chiyero cha mwezi wapitawo ndipo kutalika kwa nsambo yake fanana ndi adat yake.

Zanenedwa m'kabukhu ka **Menhel-ul-waridin** kuti **Istimrar** ikachitika kwa namwali, ndiye kuti yayambika chifukwa cha chimodzi mwa zifukwa zinayi izi:

1- Ngati magazi otulukawo akugwirizana, masiku khumi oyambilira adzavomerezeka kukhala nsambo, pomwe masiku makumi awiri otsatira pambuyo pake adzakhala masiku a chiyero.

2- Namwali akakumana ndi istimrar atatha nthawi yotuluka magazi a sahih motsatizana ndi nthawi ya chiyero cha sahih, namwaliyo wakhalano mkazi wa adat ina yake. Mwachitsanzo, ngati anatuluka magazi kwa masiku asanu ndikutsatira masiku makumi anayi a chiyero, masiku asanu oyambilira a istimrar adzavomerezedwa kukhala nsambo, masiku makumi ndi anayi otsatirawo adzakhala masiku a

chiyero. Lamuloli limagwira ntchito mpaka kutuluka kwa magazi kutasiya.

3- Ngati akudutsa m'nyengo yotaya magazi ya fasid motsatizana ndi nthawi ya chiyero cha fasid, nthawi yonseyo siyidzavomerezedwa kukhala nsambo. Ngati chiyerocho chidali cha fasid chifukwa chinali chachifupi kochepera masiku khumi ndi asanu, magazi omwe awoneka koyambako adzavomerezedwa kusanduka istimrar. Ngati magazi atuluka kwa masiku khumi ndi limodzi kutsatira masiku khumi ndi anayi a chiyero kenako kuchucha magazi kosalekeza kotchedwa istimrar; nthawi yoyamba yotaya magaziyo imakhala fasid chifukwa yadutsa masiku khumi. Tsiku la khumi ndi limodzi lakutuluka kwa magazi ndi masiku asanu oyambilira a istimrar zidzawonjezedwa ku nthawi ya chiyero, ndipo kuchokera tsiku lachisanu lowonjezerapo idzakhala adat ya masiku khumi a nsambo wotsatiridwa ndi masiku makumi awiri a chiyero. Ngati chiyero chiri chokwanira koma chiri fasid chifukwa pali masiku otuluka magazi osakanizika, ndiye kuti magazi oyambawo adzavomerezedwa kukhala istimrar, ngati kuchuluka kwa masiku a chiyero cha fasid ndi masiku akutuluka magazi sikupitirira makumi atatu. Ngati masiku khumi ndi limodzi akukha magazi akutsatirana ndi masiku khumi ndi asanu a chiyero ndipo pambuyo pake istimrar ikutsatira. Nthawi ya masiku khumi ndi asanu ndi limodzi ndi nthawi ya chiyero cha fasid chifukwa tsiku lake loyamba ndi la magazi. Masiku anayi oyamba a istimrar ndi masiku a chiyero. Ngati chiwerengero chawo chonse chadutsa masiku makumi atatu, masiku khumi oyambilira amavomerezedwa kukhala nsambo ndipo masiku onse mpaka istimrar amavomerezedwa kukhala masiku achiyero, pomwe masiku khumi mozungulira a nsamboakutsatidwa ndi masiku makumi awiri achiyeroadzakhazikidwa. Lamuloli limagwira ntchito pamene masiku khumi ndi limodzi akukha magazi akumatsatidwa ndi masiku makumi awiri a chiyero ndipo pambuyo pake kumayamba istimra.

4- Akadutsa m’magazi a sahih ndi kukhala chiyero cha fasid, masiku otuluka magazi a sahih ndi nsambo, pomwe kenako kubwera masiku makumi atatu (30) omwe avomerezrdwe kukhala oyera. Mwachitsanzo, ngati istimrar ichitika patatha masiku asanu okutuluka magazi ndi kutsatira masiku khumi ndi anayi a chiyero, masiku asanu oyamba ndi nsambo ndipo masiku makumi awiri ndi asanu otsatirawo ndi masiku a chiyero. Masiku khumi ndi limodzi oyambilira a istimrar amavomerezedwa ngati masiku a chiyero kuti agwirizane ndi chiwerengero kufika pa makumi awiri ndi asanu. Kuyambira

pamenepo, masiku asanu a nsambo kuphatikiza masiku makumi awiri ndi asanu a chiyero adzatsatizana. Chimodzimodzinso, ngati istimrar ichitika patatha masiku atatu akutuluka magazi, kutsatiridwa ndi masiku khumi ndi asanu akuyeretsedwa, kenako ndi tsiku limodzi lakukha magazi, kenako ndi masiku khumi ndi asanu a chiyero; masiku atatu oyamba kutuluka magaziwo kukhala masiku nsambo, masiku onse mpaka tsiku la istimrar adzavomeredwa monga masiku a chiyero; potero, nthawi yake idzakhal masiku atatu a nsambo ndi masiku makumi atatu ndi limodzi a chiyero. Mu nthawi ya istimrar, masiku atatu a haid ndi masiku makumi awiri ndi asanu ndi awiri a chiyero adzatsatizana.

Ngati nthawi yachiwiri ya chiyero ikatakhala masiku khumi ndi anayi, kukha magazi kudzavomerezedwa kukhala kuti nkosalekeza malinga ndi Imam Abu Yusuf, kotero masiku awiri oyambilira m'masiku khumi ndi anayiwo adzaphatikizidwa ku tsiku limodzilo mmasiku khumi ndi anayiwo monga masiku a nsambo ndi kutsatiridwa ndi masiku khumi ndi asanu (15) achiyero, ndi zina zotero. Poti, masiku atatu oyamba akukha magazi otsatidwa ndi masiku khumi ndi asanu a chiyero okhala mu nthawi ya sahih, adzavomerezedwa ngati adat.

Mkazi amene wayiwala nthawi ya adat yake amatchedwa **muhayyira** kapena **dalla**.

Nifas ndi kuchucha magazi pambuyo pakubere. Magazi amene amatuluka mzimayi akapita padera ndi nifas ngati manja, mapazi, ndi mutu za mwanayo zinapangika. Sitinganene nthawi yochepetsetsa ya nifas. Kutaya magazi kukatha, amachita ghusl ndi kuyambanso namaz yake za tsiku ndi tsiku. Koma, sangayambe kukhalira limodzi ndi mwamuna wake masiku olingana ndi adat yake asanakwane. Kutalika kwa nifas ndi masiku makumi anayi. Tsiku la 40 likatha, amachita ghusl ndikuyamba kuchita namaz yake ngakhale magazi asanathe. Magazi amene amatuluka pambuyo pa tsiku la makumi anayi ndi istihada (Nsambo yokakamira). Ngati mkazi apezeka kuti ali mchiyero patanggotha masiku makumi awiri ndi asanu atabereka mwana wake woyamba, adat yake ndi makumi awiri ndi asanu. Ngati mkaziyo ataya magazi kwa masiku makumi anayi ndi asanu atabereka mwana wake wachiwiri, masiku a nifas yake adzawerengedwa ngati masiku makumi awiri ndi asanu ndipo masiku makumi awiri otsalawo ndi istihada. Amachita qada namaz zake zomwe sadachite m'masiku makumi awiriwo. Ndi chifukwa chake, ayenera kuloweza masiku a nifas. Ngati magazi asiya, mwachitsanzo, m'masiku makumi atatu ndi asanu m'malo mwa masiku makumi anayi ndi asanu, masiku onse makumi

anayi ndi asanu ndi nifas, ndipo masiku ake asintha kuchoka pa masiku makumi awiri ndi asanu kufika makumi atatu ndi asanu.

Ngati, mu Ramadhan, mkazi wasiya kusamba kapena kutuluka magazi pa nifas nthawi ya sahur (m'bandakucha), itangatha, iye sadya kapena kumwa pa tsikulo. Koma Ramadan ikatha adzchita qada ya kusala kwa tsiku limenelo. Ngati haid kapena nifas zitayamba nthawi ya sahur itadutsa, kaya madzulo, amadya ndi kumwa tsiku limenelo.

M'masiku a haid kapena nifas, m'ma Madhhab anayi onse, ndi haram kwa mkazi kuchita Namaz, kusala kudya, kulowa mu mzikiti, kuwerenga kapena kugwira Qur'an al-kareem, kuchita tawaf (kuzungulira Ka'ba-i-mu'azzama mkati mwa Masjid-i-haram), ndi kugonana. Adzachita qada kusala kwake, koma osati namaz yake. Namaz yake amakhululukidwa. Ngati nthawi ya Namaz achita ercemewudhu, ndi kukhala pa nswala wake mongati momwe akanakhalira akuchita Namaz, ndikuchita dhikr ndi kunena ma tasbih; eye dzapeza thawab ngati momwe akanapezera atachita Namaz yake ya bwinobwino.

Bukhu la **Jawhara-t-unneyyira** lafotokoza motere:[1] "Mkazi azidziwitsa mwamuna wake kuti haid yake yayamba. Pamene mwamuna wake afunsa, lidzakhala tchimo lalikulu kwa iye kusamuuza. Adzakhalanso wochimwa kwambiri ngati anganene kuti haid yake yatha, ngati chiyero chake chikupitilirabe. Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Mkazi amene akubisira mwamuna wake chiyambi ndi mapeto a haid yake ndi wotembeleredwa."** Ndi haram kugonana ndi mkazi wako kumalo otulukira chimbudzi pa nthawi yomwe ali pa nsambo ngakhale ali bwino. Ndi tchimo lalikulu. Munthu amene wachita tchimo limeneli ndi mkazi wake ndi wotembereredwa. Kuchita za chikondi pakati pa anthu awiri a ziwalo zobisika zofanana ndi tchimo lalikulu kwambiri. Imatchedwa **liwata**, ndipo imanenedwa kukhala **habith** (chonyansa kwambiri) mu Surah Anbiya. Monga momwe anafotokozera **Birgivi**, Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" adati: "**Ngati muwapeza anthu awiri akuchita zoipa monga momwe anthu a Luti adachitira, apheni onse awiriwo!** Malinga ndi akatswiri a Chisilamu ena, onse awiri ayenera kuwaotcha moto. Onse awiri amasanduka junub akachita nyansi imeneyi. Kulowetsa kwa

[1] Chidule cha mabuku atatu otchedwa Siraj-ulwahhaj, lomwe Abu Bakr bin 'Ali Haddad-i-Yemeni "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (d. 800 [1397 AD]) adalemba ngati ndemanga ya Mukhtasar -i-Quduri, lomwe linalembedwa ndi Abul-Huseyn Ahmad bin Muhammad Baghda "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih"(362 [973 AD] - 428 [1037], Baghdad).

mankhwala a madzimadzi ochititsa kuti chimbudzi chituluke sikungachititse kuti munthu akhale wa junub, ngakhale kuti zimaononga kusala kwake (Feyziyya). Ngati mkazi aona kuti haid yake yayamba mkati mwa nthawi ya Namaz yomwe sadachitebe, sangachite qada ya Namaz imeneyo.

UDHU kapena KUZITSUKA

Udhu uli ndi ma fardh anayi (4) malinga ndi Madhhab a Hanafi, ma fardh asanu ndi awiri (7) m'Madhhab a Maliki, ndi ma fardh asanu ndi limodzi (6) m'Madhhab a Shafi'i ndi Hanbali. Malinga ndi Madhhab a Hanafi ma fardh ali motere:

1- Kusukusula Khope.

2- Kusamba m'manja mpaka pa mfundo ya chikhato.

3- Kuchita masah (kupaka madzi) pa gawo limodzi mwa magawo anayi a mutu.

4- Kusambitsa mapazi mpaka mu chidendene. Pali mitundu itatu ya Udhu: Umodzi mwa mitunduyi ndi fardh, wachiwiri ndi wajib, wachitatu ndi Sunnah, ndipo wachinayi ndi mandub.

Pali zochitika zinayi zofunika kuti udhu wa fardh ukhalepo: Kupanga udhu woti mugwire Qur'an al-kareem kapena kuswali imodzi mwa ma namaz asanu a pa tsiku, kapena kuchita namaz ya janaza.

Udhu wa wajib ndi womwe umachitikira pa tawafi-ziyarat.

Udhu wa Sunnah ndi omwe umachitika pofuna kuwerenga Qur'an al-kareem (popanda kuyigwira) kapena kukazonda ku manda a Asilamu, kapena kuchita udhu musanachite ghusl.

Udhu wa mandub ndi omwe umachitika musanagone komanso/kapena mukadzuka. Ngati mwanena bodza kapena miseche (kunena munthu wina) kapena kumvera nyimbo zodzutsa zilakolako, ndi mandub (kofunikira) kuchita tawba ndi istighfar pa utchimo womwe mwachita kenako ndi kuchita Udhu.

Ndi mandub kuchita udhu pomwe mukupita kukamvera ilm (kudziwa) kapena kubwereza udhu ngakhale kuti munachita kale, koma mwina mwachita chinthu chomwe sichikanaloledwa kuchitika musanachite udhu, [Mwachitsanzo ngati mwachita namaz.] Ngati simudachite mapempherowo (ndi udhu omwe munachita), ndi makruh kuchita udhu ngakhale muli ndi udhu.

ZA MADZI

Pali mitundu inayi ya madzi: Ma-i-mutlaq; ma-i-muqayyad; ma-i-meshkuk ndi ma-i-musta'mal.[1]

1- Zitsanzo za ma-i-mutlaq ndi madzi a mvula, madzi a m'nyanja, akasupe, ndi madzi a pa chitsime. Madzi amtundu uwu amakhala ndi kuthekera koyeretsa zinthu zakuda. Atha kugwiritsidwa ntchito pa ntchito iliyonse.

2- Zitsanzo za ma-i-muqayyad ndi madzi a mavwembe, madzi a mpesa, madzi a maluwa, ndi zina zotero. Madzi amtundu uwu alinso ndi kuthekera koyeretsa zinthu zauve, ngakhale kuti sizotheka kuchitira udhu kapena ghusl.

3- Madzi otsala bulu atamwa kapena chakumwa cha chinyama chobadwa kwa hatchi koma mayi wake ndi bulu amatchedwa ma-i-meshkuk. Ndizololedwa kuchitira udhu ngakhale ghusl madzi amenewa. Munthu ali ndi chisankho chochita chimodzi chisanadze chinzake.

4- Zoti madzi amakhala ma-i-musta'mal akagwera pansi kapena pamene akuchoka pa chiwalo chomwe chikutsukidwa ndi funso lomwe limavuta pakati pa akatswiri a Chisilamu. Makamaka amasanduka akamachokera pa chiwalo chotsukidwa, - fatwa ikugwirizana ndi ijtihad (kumasulira) imeneyi. Potengera izi, pali ma qawl (kulongosola komwe ma mujtahid amatanthauzira ma ijtihad zawo.) atatu osiyana. Malinga ndi Imam Azam (Abu Hanifa) "rahima-hullâhu ta'âlâ", ndi najasat-i-ghaliza (qaba najasat). Malinga ndi Imam Abu Yusuf "rahima-hullâhu ta'âlâ", ndi najasat-i-khafifa. Ndipo malinga ndi Imam Muhammad "rahima-hullâhu ta'âlâ", ndi oyera. Qawl yomalizayi ndi yokhazikika (malinga ndi fatwa yomaliza).

Udhu kuti ukhale wujub (ukhalepo), zinthu zisanu ndi zinayi (9) ziyenera kukwaniritsidwa:

1- Kukhala Msilamu.

2- Kukwanitsa zaka zakutha msinkhu.

3- Kukhala wa nzeru zake.

4- Kukhala wopanda udhu.

5- Kuti madzi (ogwiritsa ntchito) akhale oyera.

6- Kutha kuchita udhu.

7- (Kwa mkazi) osakhala nthawi yosamba (nsambo).

[1] 'Ma' kutanthauza madzi'.

8– (Kwa mkazi) asakhale mu nthawi yoti angobereka kumene.

9- Pa pemphero lirilonse m'mapephero asanu a pa tsiku, nthawi ya Namaz ikakwana. [Izi zimagwira ntchito kwa munthu amene ali ndi udhr].

MA SUNNAH A UDHU: Anenedwa ma Sunnah makumi awiri ndi asanu (25).

1- Kunena kuti, "Audhu... " (kumaliza kwake ndi: "Audhu billahimin-ash-shaytan-ir-rajim."

2- Kunena kuti Bismilla (kunena kuti: "Bismillah-ir-Rahmanir-Rahim.")

3- Kusamba m'manja

4– Kuchita khilal pakati pa zala, komwe ndi kutsuka pakati pa zala pogwiritsa ntchito zala za m'manja ngati mano a chipeso pakati pa zala za dzanja lina)

5– Kuthira madzi m'kamwa.

6- Kuthira madzi m'mphuno

7- Kuchita niyyah (kutsimikizira). M'madhhab a Hanafi, kuchita niyyah pakutsuka mkamwa ndi Sunnah osati fardh. Koma ndi fardh m'adhhab a Shafi'i. M'madhhab a Maliki ndi fardh kuchita niyyah posamba m'manja.

8– Kuyang'ana ku Qibla

9- Kuchita khilal ku ndevu zanu pogwiritsa ntchito zala zanu ngati chipeso (ngati zili zochuluka.)

10– Kuchita masah pa ndevu zanu.

11– Pochita chirichonse kuyamba ndi mbali ya dzanja lanu la kumanja

12– Kuchita khilal pakati pa zala za ku phazi ndi chala cha ching'ono cha kumanzere, kuyambira pansi pa chala chaching'ono cha phazi la kumanja.

13- Kuchita masah pamutu –ponyowesa mutu (wonse).

14- Kuchita masah m'makutu ndi ku nkhonkho, pogwiritsa ntchito madzi otsala pa mutu.

15- Kusunga tertib, kunena kuti kusambitsa ziwalo zoyenera kusambitsa potsata ndondomeko yoyikidwa.

16– Osalekeza, mukayamba chiwalo choyamba mpaka kumaliza kusambisa ziwalo zonse, chimodzi pambuyo pa chinzake.

17- Pochita masah pa mutu, kuyamba ndi gawo la kutsogolo.

18- Kugwiritsa ntchito miswak (mswachi).

19- Kunyowetsa m’mbali mwa maso ndi nsidze.

20- Delk, kunyula ziwalo modekha ndi manja anu.

21- Kuchita udhu mutayima malo okwelerako.

22- Kutsuka chiwalo chilichonse katatu.

23- Kuthiramonso madzi ena abwino mkaapu yomwe mumachitira udhu.

24- Kusayankhula zinthu za pa dziko pamene mukuchita udhu.

25- Kusunga niyyah yanu.

KUGWIRITSA NTCHITO MISWAK (MSWACHI)

Pali zopindula khumi ndi zisanu (15) pogwiritsa ntchito miswak. Zopindulitsa zimenezi malinga ndi bukhu lotchedwa Siraj-ul-wahhaj (ndemanga yomwe ili mmagawo atatu yolembedwa ndi Abu Bakr bin Ali Haddad Yamani “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih”, d. 800 [1397 AD], pa bukhu lotchedwa Mukhasar -i-Quduri, limenenso linalembedwa ndi Abul Hueyn Ahmad bin Muhammad Baghdadi “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih”, 362 [973 AD] - 428 [1037], Baghdad), ziri motere:

1- Zidzakuthandizani inu kunena Kalima-i-shahadat po mwalira.

2- Nkhama zanu zimakhala zolimba.

3- Zimathandiza kumasula makhololo osafunika m'chifuwa mwanu. (miswak ndi mchotsa makhololo wa bwino)

4- Zimaletsa kutuluka mowonjeza kwa ndulu.

5- Kumachepetsa ululu wa mkamwa.

6- Kumachotsa mpweya woipa.

7- Allahu ta’âlâ amamusangalalira munthu wogwiritsa ntchito miswak.

8- Kumalimbitsa mitsempha ya pa khosi.

9- Satana mdyerekezi amakhala wokhumudwa ukagwiritsa ntchito miswak.

10- Maso anu amawala ndi nur mukagwiritsa ntchito miswak.

11- Kumachulukitsa ntchito zanu zopembedza, khayr ndi hasanat (zaukhondo ndi zabwino).

12- Mumakhala kuti mwachita mchitidwe wa Sunnah pogwiritsa ntchito miswak.

13- Pa kamwa panu pamakhala poyera.

14- Zoyankhula zanu zimakhala zomveka.

15- Ma rakaat awiri a namaz yochita mutatsuka mano ndi miswak amakupezetsani thawab zochuluka kuposa ma rak'at makumi asanu ndi awiri (70) a namaz ochitika musanagwiritse ntchito miswak.

MA MUSTAHAB A UDHU

Ma mustahab (zolimbikitsidwa) a udhu alipo asanu ndi imodzi motere:

1- Osanena ndi lirime lanu niyyah imene mukuchita mumtima mwanu.

2- Kuchita masah ku nkhonkho ndi madzi otsala m'makutu mwanu.

3- Osasambitsa mapazi anu moyang'anitsa ku Qibla.

4- Kumwa, ngati kuli kotheka, madzi otsalira pa udhu, mutayimilira kuyang'ana ku Qibla.

5- Kuwaza madzi pa zovala zanu mukamaliza udhu.

6- Kupukuta ziwalo zomwe mwasambitsa ndi chopukutira choyera.

Ibni Abidin akunena motere pa zomwe zingaononge udhu: "Ngati chinthu chomwe si makruh m'Madhhab mwanu chili fardh m'Madhhab ena, amodzi mwa Madhhab atatuwo, ndiko kuti ndi mustahab kwa inu kuchita." Imam Rabbani akunena mu kalata yake ya mazana awiri mphambu makumi asanu ndi atatu kudza zisanu ndi chimodzi (286) kuti: "Chifukwa ndi fardh mu Madhhab a Maliki kusambitsa ziwalo zomwe zimasambitsidwa pa nthawi ya udhu mofatsa ndi dzanja, ife, a Madhhab a Hanafi monga momwe tiliri, tiyenera kusisita." Ibni Abidin akunena motere monga momwe akulongosolera talaq-i-rij'i kuti: "Ndi zolimbikisidwa kwa Msilamu wotsata Madhhab a Hanafi kutsanzira Madhhab a Maliki. Pakuti, Imam Malik, (mtsogoleri wa Madhhab a Maliki,) ali ngati wophunzira wa Imam Azam Abu Hanifa, (mtsogoleri wa Madhhab a Hanafi).

Pamene akatswiri a Madhhab a Hanafi sanathe kupeza qawl mu Madhhab a Hanafi (kuti athetse vuto lina lake), anapereka fatwa yawo yomaliza molingana ndi Madhhab a Maliki. Mwa ma Madhhab (ena atatuwo) Madhhab a Maliki ndi omwe ali ogwirizana kwambiri ndi Madhhab a Hanafi."

MAKRUH A UDHU

Makruh (zonyansa) zpa udhu zilipo khumi ndi zisanu ndi zitatu (18) motere:

1– Kuwaza–madzi–molimba pa nkhope panu.

2- Kupumira m'madzi omwe mukugwiritsa ntchito pochita udhu.

3- Kusambitsa ziwalo kamodzi kapena kawiri mmalo mwa katatu.

4- Kusambitsa ziwalo koposa katatu.

5- Kulavulira m'madzi omwe mukugwiritsa ntchito pochita udhu.

6- Kuminira m'madzi omwe mukugwiritsa ntchito pochita udhu.

7- Kulola madzi kulowa ku mmero kwanu pamene mukugwedeza madzi kummero.

8- Kutembenuzira msana wanu ku Qibla (pochita udhu).

9- Kutsinzina kwambiri.

10- Kutong'ola maso anu.

11– Kuyamba kuchita udhu ndi mbali ya ku manzere.

12- Kumina pogwiritsa ntchito dzanja lanu la manja.

13- Kugwiritsa ntchito dzanja la manzere potsira madzi mkamwa mwanu.

14- Kugwiritsa ntchito dzanja lanu la manzere popaka madzi mphuno mwanu.

15- Kumenyesa phazi lanu pansi.

16- Kuchita udhu ndi madzi otenthetsa pa dzuwa.

17- Kusapewa kugwiritsa ntchito madzi a ma-i-musta'mal. (Chonde onani mitundu ya madzi kumayambiliro kwa nkhaniyi.)

18– Kuyankhula nkhani zocheza za padziko mukuchita udhu.

ZOMWE ZIMAWONONGA UDHU

Zilipo makumi awiri ndi zinayi (24) zomwe zatchulidwa:

1- Zinthu zomwe zimatuluka ku kumbuyo.

2- Zinthu zomwe zimatuluka ku kutsogolo kwanu.

3- Nyongolozi, miyala kapena zina zotere zomwe zimachokera kutsogolo kapena kumbuyo.

4- Kulowetsa kapena kulowetsedwa chinthu kotulukira chimbudzi.

5- Ngati mankhwala omwe mkazi anabayadwa m'mimba mwake atabwelera.

6- Ngati mankhwala amene wathira m'khutu atulukira mkamwa mwake, amawononga udhu wake. Ngati atatulukira m'khutu kapena m'mphuno samaononga udhu wanu (Fatawa-i-Hindiyya)

7- Ngati thonje lomwe mzibambo walowetsa kokodzera kwake likunyowa ndi kugwa. [Ngati kathonjelo lili kunja kwa ngalande yotulukira nkodzo ndipo mbali yomwe ili kunjayo ndi youma, udhu siunaduke bola kasagwe.]

8– Ngati kathonjeko kagwa pansi ndipo mbali yotsalira panja ndi yonyowa.

9- Kusanza zinthu zodzadza m'kamwa. Makhololo saononga udhu ngakhale atakhala ochuluka. Dovu lotuluka m'kamwa mwa munthu akugona ndi la ukhondo, ngakhale litakhala la chikasu.

10- Kukhetsa misozi chifukwa cha kudwala kumawononga udhu. Koma misozi yotuluka chifukwa cha kulira, mphamvu ya zinthu monga utsi, anyezi ndi zina zotero sikuwononga udhu.

11- Magazi, mafinya, kapena madzi achikasu otuluka mphuno mwa munthu amaononga udhu. Mamina si najs (nyansi) ndipo sawononga udhu wa munthu akatuluka mphuno.

12- Kulavula malovu okhala ndi magazi ambiri.

13- Kuona magazi pa chinthu chomwe mwaluma kumene kumawononga udhu wanu ngati mkamwa kapena mano anu apakika ndi magaziwo. Koma ngati sanapakike, udhu wanu uli bwino.

14- Mukaona kuti magazi atuluka pa chiwalo chili chonse ndi kufalikira pa chiwalopo, ngakhale athakhala ochepa, udhu wanu udzaonongeka ngati mukutsatira Madhhab a Hanafi. Koma ngati mukutsatira Madhhab a Maliki ndi Shafi'i, udhu wanu siunaonongeke.

15- Tiyerekeze mwakwera hatchi yopanda chokhalira (sadulo); inu ndi kumawodzera ikutsetsereka chitunda, udhu wanu wawonongeka.

16- Ngati mukukayikira kuti muli ndi udhu kapena ayi, dhann-i-ghalib (maganizo anu) akhale oti mulibe udhu.

17- Ngati mwamuna atakumbatira mkazi wake ali maliseche, udhu wawo udzaonongeka.

18- Ngati mwayiwala kusambitsa chiwalo chanu chimodzi ndipo simukukumbukira kuti ndi chiti, udhu wanu udzakhala opanda pache.

19. - Mafinya, magazi, kapena madzi achikasu akatuluka pa thuza pa chiwalo chanu, pa okha kapena mutafinya, udhu wanu udzawonongeka.

20- Tiyerekeze kuti muli ndi chilonda, chomwe chiri ndi najs monga, madzi achikasu, magazi kapena mafinya pakati pake, udhu wanu udzaonongeka pamene mbali ya thupi lanu ya bwino ikhudzidwa ndi thonje kapena bandeji lomwe liri pa chilondapo itapakidwa ndi najs. Akatswiri amanena kuti madzi opanda mtundu otuluka m'chilonda kapena chiphuphu sangawononge udhu wa munthu. Ndi zololedwa kwa anthu amene akudwala matenda monga kuyabwa, nthomba ndi chikanga kutsatira mawu amenewa.

21- Tiyerekeze kuti mwasinza mutatsamira chinachake; udhu udzaonongeka ngati tulo lanu liri lakuya kwambiri koti mungagwe ngati wina atachotsa chinthu chimene mwatsamiracho.

22- Mu Namaz, pa nthawi ya ruku ndi ma sajda, kuseka mokweza koti iwe mwini kapena munthu wayandikana naye ndi kumva. Ngati museka koti wina aliyense sangamve kupatula inu, udhu wanu uli bwino, koma kuti Namaz yomwe mukuchita idzakhala yopanda pake. Kutanthauza kuti kuseka mokweza kongomva iwe wekha kumaononga Namaz koma osati udhu.

23- Kugwa khunyu kapena kukomoka kumawononga udhu.

24- Ngati mafinya, madzi achikasu kapena magazi akutuluka m’khutu ndi kufika pa mbali ya thupi lanu yomwe mukuyenera kuthira madzi pochita ghusl, udhu wanu udzawonongeka.

Anthu aku Ulaya anaphunzira kusamba kwa pa gulu kuchokera kwa ife. Asanaphunzire kuchokera kwa ife, nyumba zawo zinali kununkha kwambiri moti munthu ankamva kununkha akakupumira. Ndi Asilamu omwe anafalitsa ukhondo pa dziko lonse lapansi, potero anapulumutsa mtundu wa anthu kwa mdani wowawa kwambiri, umve.

MAPEMPHERO ONENA POCHITA UDHU

Poyamba kuchita udhu nenani kuti: **"Bismillah-il" adhim wa-l-hamd-u-li-l-lahi 'ala din-il-islami wa' ala tawfiq-ilimani al. -hamd-u-li-l-lah-il-ladhi ja'al-al-maa tahuran wa ja'al-alislama nuran."**

Pamene mukuthira madzi mkamwa mwanu mumati: **"Allahummasqini min hawdi nabiyy-ika ke'sen la 'azmau ba'dehu abadan."**

Mukamapaka madzi mphuno mumati: **“Allahumma arihni rayiha-t-al Jannati wa-r-zuqni min naimiha wa la turihni rayihatan-nari.”**

Pamene mukusambitsa nkhope yanu mumati: **“Allahumma bayyid wajhi binurika yawma tabyaddu wujuhu awliyaika wala tusawwid wajhi bizunubi yawma taswaddu wujuhu a’daika.”**

Pamene mukusambitsa mkono wanu wa kumanja (kuphatikiza chigongono) mumati: **“Allahumma a’tini kitabi bi-yamini wa hasibni hisaban yasiran.”**

Pamene mukusambitsa mkono wanu wa kumanzere (kuphatikiza chigongono) mumati: **“Allahumma la tu’tini kitabi bishimali wa la min warai zahri wala tuhasibni hisaban shadidan.”**

Pamene mukuchita masah pa mutu panu mumati: **“Allahumma harrim sha’ri wa beashari ’alannari wa azilleni tahta dhilli ’Arshika yawma la dhilla illa dhilluka.”**

Pamene mukuchita masah m’makutu mwanu mumati: **“Allahumma-j’alni minalla-dhina yastami’una-l-qawla fa yattabi’una ahsanah.”**

Pamene mukuchita masah kunkhonkho kwanu mumati: **“Allahumma a’tik raqabati min-an-nari wahfaz min-as-salasili wal-aghlal.”**

Pamene mukusambitsa phazi la kumanja mumati: **“Allahumma thabbit qadamayya ’ala-s-sirati yawma tazillu fihil-aqdam.”**

Mukamasambitsa phazi la kumanzere mumati: **“Allahumma la-tatrud qadamayya ’ala-s-sirati yawma tatrudu kullu aqdami a’daika. Allahumma-j’al sa’yi mashkuran wa zanbi maghfuran wa ’amali maqbulan wa tijarati len’tebura.”**

Mukamaliza kuchita udhu wanu mumati: **“Allahumma-j’alni min-at-tawwabina wa-j’alni min-almutatahhirina wa-j’alni min ’ibadika-s-Saalihina wa-j’alni min-alladhina la khawfun ’alaihim wala hum yahzanun.”**

Kenako, maso anu atalunjika kuyang'ana ku mwamba ndipo mumati: **“Subhanakallahumma wa bihamdika ash-hadu an la ilaha illa Anta wahdaka la sharika laka wa anna Muhammadan ’abduka wa rasuluka.”**

Kenako munene Sura ya **Inna anzalna** kamodzi kapena kawiri kapena katatu. Muyambe Surayi ponena kuti, **"Bism-illah-ir-Rahman ir-Rahim,"**.

Ndikofunika kuphunzira maphunziro a chipembedzo amene banja lanu ndi ana anu afunika kuphunzira ndikuwaphunzitsa. Tsiku la Kiyama amuna adzafunsidwa za akazi awo.

ZOKHUDZA TAYAMMUM

Malinga ndi Madhhab a Hanafi, tayammum idzakhala sahih nthawi yopemphera isanakwane. Koma si sahih kwa Madhhab ena atatuwo.

Mu tayammum muli ma fard Zitatu: Tayammum yomwe imafunika pochita udhu ndi chimodzimodzi ndi tayammum yofunikira pochita ghusl. Zimangosiyana ma niyyah awo (zitsimikizo zawo). Choncho, ma tayammum awiriwa sangagwiritsidwe ntchito mosinthana.

1- Kuchita niyyah, yomwe ndi yokakamizidwa.

2- Kukhudza nthaka ndi manja onse awiri kenako kuchita masah kumaso konse. Manja akhudze pa nkhope yonse.

3- Kukhudza nthaka ndi zikhato zonse ziwiri kachiwiri, kenako nkuchita masah pa nkono wanu wonse wa ku manja ndi dzanja lanu la manzere kenako chitani masah nkono wanu wa kumanzere pogwiritsa ntchito dzanja lanu la manja, kuphatikiza zigongono. Zochita zonse ndi rukns, (ndi fard mu tayammum). Ngati china sichinachitike, tayammamu idzakhala yopanda phindu).

Umboni wa m'mabuku kuti tayammum ndi fardh ndi ayah 43 ya Surah Nisa ndi ayah yachisanu ndi chimodzi (6) ya Surah Maida. M'Madhhab a Maliki ndi Shafi'i, nkosaloledwa kuchita tayammum, pofuna kuchita namaz, nthawi yake ya Namaz isanakwane. Ndipo tayammum siingathe kugwiritsidwa ntchito mu namaz yoposa imodzi. Apa tikufuna kunena kuti mudzafunika kuchita tayammum yatsopano pa Namaz iliyonse, ndipo mudzachita nthawi yake yoyikidwa ya Namaz imeneyo itakwana.

Pali zinthu zisanu ndi chimodzi zomwe sizikuloledwa kuchitira tayammamu, pokhapokha ziri ndi dothi la fumbi. Zinthu zisanu ndi chimodzizi ndi izi: Zitsulo za ironi, za kopala, za buronzi, za tini, za golide, za siliva, ndi zitsulo zina zonse. Tayammum ikuloledwa ndi china chirichonse kupatula zitsulo izi, zomwe zimasungunuka zikatenthedwa; galasi, lomwe limafewa likatenthedwa; ndi matayilosi wonyezimira. Zinthu ziyenera kukhala ndi dothi.

Dothi lomwe munthu wakodzerapo mutha kuchitirapo namaz likauma. Koma simungachite tayammum ndi dothi limenelo. Kuti tayammum ikhale yololedwa, pakufunika kuti mufunefune madzi, ndipo musawapeze. Ndiye mufunse Msilamu wa adil and Salih. (Adil ndi yemwe sachita tchimo lalikulu ndipo sachita matchimo mwachizolowezi ndipo Salih ndi Msilamu amene amapewa za haram ngakhale zokayikitsa ndipo amalakwa mosadziwa.)

Pali zofunikira zisanu zomwe ziyenera kukwaniritsidwa pochita tayammum:

1- Kuchita niyyah. 2- Kuchita masah. 3- Kuti chinthucho chigwiritsidwe ntchito pochita tayammum chiyenera kukhala cha dothi. Ngati sichinapangidwe ndi dothi, chiyenera kukhala ndi fumbi la dothi. 4- Chinthu chadothi kapena chokhala ndi fumbi chomwe chikugwiritsidwa ntchito pa tayammum chiyenera kukhala chaukhondo. 5- Zikhale kuti mwalepheleratu kupeza madzi ogwiritsa ntchito pochita udhu. [Kufooka kapena kudwala matenda ena ake ndi udhr, potero ukhoza kuchita tayammum ngati kugwiritsa ntchito madzi kungayambitse mavuto. Chimodzimodzi kufooka ndi ukalamba. Anthu omwe ali ndi zifukwa zoterezi akuloledwanso kuchita Namaz yawo atakhala.]

Pali ma Sunnah asanu ndi awiri (7) zomwe ayenera kutsatidwa pochita tayammum:

1- Kunena “Bismillah-ir Rahman ir-Rahim,” pamene mukuyamba kuchita tayammamu. 2– Kumenya zikhato za manja modekha pa nthaka ya ukhondo. 3- Kusisita chinthu chomwe mukuchitira tayammum modekha poyendetsa manja anu kutsogolo ndi kumbuyo kamodzi. 4- Kutambasula zala. 5- Kusasa fumbi m'manja. 6- Kuyamba kuchita masah pa nkhope. 7-Kuchita masah mikono yanu mpaka zigongono.

Pali zinthu zinayi zoyenera kukwaniritsa pofunafuna madzi.

1- Kuti malo omwe muli ndi oti amakhalako anthu.

2- Ngati mwadziwitsidwa za kupezeka kwa madzi.

3- Ngati mwatsimikiza kuti madzi alipo.

4- Ngati simuli pamalo owopsa.

Ngati munthu wapeza madzi koma patali kwambiri koposa mayilo imodzi, ndi kololedwa kwa munthu ameneyo kuchita tayammam mmalo mopita kukachita udhu. Koma ngati mtunda uli wosakwana mayilo imodzi, ndipo kuti munthu atha kukafika ndi kubwera nthawi ya Swalah isanathe, sikudzakhala kololedwa kuchita tayammamu. [mayilo imodzi ndi mtunda wa zra zikwi zinayi, ndiye kuti 0.48 x 4000 = 1920 mamita mu Madhhab a Hanafi.]

Koma tiyerekeze mwafuna madzi ndipo mwalephera kuwapeza, ndi kuchita tayammum ndi kuchita Swalah. Mutamaliza kuchita Swalah ndi kuwaona madzi, kodi padzafunika kubwereza Swalahyo? Ili ndi funso lomwe akatswiri a Chisilamu anakambirana. Yankho

lotsimikizika ndi loti sipadzafunika kubwereza Swalah yomwe wachita kale.

Ngati munthu atanyowa koma palibe madzi ndi kuchitira udhu ndipo palibe chinthu chouma choti agwiritse ntchito pochita tayammum, ayenera kuumitsa matope ndi kuwachitira tayammum. Tiyerekeze kuti anthu angapo achita tayammum aliyense; ndipo ngati mmodzi mwaiwo awona madzi, tayammum ya wina aliyense idzakhala yopanda pake.

Ngati munthu abweretsa madzi kudzalipatsa gulu ndi kunena kuti mmodzi mwa iwo agwiritse ntchito madziwo pochita udhu, tayammum zomwe gulu lonse lachita zimasanduka fasid, (zopanda pake). Koma ngati atanena kuti madziwo ndi a gulu lonse kuti lichitire udhu koma madzi operekedwawo ndi okwana udhu wa munthu mmodzi, tayammum zomwe achite onsewo zidzakhala sahih (zovomerezeka ndi zomveka).

Tiyerekeze kuti munthu ali junub[1] ndipo sangapeze madzi pali ponse koma mu mzikiti; adzayenera kuchita tayammum ya ghusl poyamba ndipo kenako alowe mu mzikiti kukatunga madzi. Koma ngati sanapezemo madzi mu mzikitimo, adzafunika kuchita tayammu ina ya Namaz.

Tiyerekeze kuti munthu atakhala mu mzikiti watuluka umuna kapena ukazi; Adzayenera kuchita tayammam ndi kutuluka mu mzikiti.

Tiyerekeze kuti munthu alibe manja; akuloledwa kuchita tayammum. Koma munthu ameneyo ayenera kuchita istinja ngati ali ndi wina womuthandiza kutero.[2] Ngati alibe womuthandiza, iye adzakhululukidwa.

Ngati munthu alibe manja ndi mapazi, adzakhululukidwa kuti asachite namaz molingana ndi Tarafayn, Imam Azam Abu Hanifa ndi wophunzira wake Imam Muhammad Shaybani. Koma malinga ndi Imam Abu Yusuf, munthu ameneyo ayenerabe kuchita namaz.

Ndi kosaloledwa kuchita tayammum pokapemphera Swala ya Jummah. Ngati munthu alibe nthawi yochite udhu wa Swala ya Jummah, sikudzaloledwa kwa iye kuchita tayammum mothamanga poopa kuti mapemphero angamudutse.

---

[1] Junub amatanthauza (m'modzi) amene akufunika kuchita ghusl pazifukwa monga kugonana komanso kutulutsa umuna kapena ukazi. Chonde onaninso mutu wokhudzana ndi ghusl.

[2] Istinja amatanthauza kuyeretsa kutsogolo kapena kumbuyo pambuyo pokodza kapena kuchita chimbudzi.

[Poti pali Swala ya masana yoti munthu ata kupemphera ngati wa phonya Jummah. Adzayenera kuswali Dhuhr.] Zalembedwanso m'buku lotchedwa **Durr-ul-mukhtar** kuti siziri zololedwa kuchita udhu ndi 'nebidh' (msuzi wa tende).

Ngati munthu aziganizira ndikutulutsa umuna kapena ukazi ali paulendo, ayenera kuchita tayammum ndikupemphera pemphero lake la m'mawa. Kenako apitilire ndi ulendo wake mpaka masana. Kutatsala nthawi pang'ono kuti Swala ya masana ithe, ayenera kuchita tayammum ndi kuswali Swala ya masanayo. Tiyerekeze kuti munthu ameneyu wapeza madzi masana a tsikulo, kodi afunika kubwerezanso mapemphero ake a m'mawa ndi a masana? Akatswiri a Chisilamu sanagwirizane pa funsoli. Koma malingana ndi qawl imodzi, iye adzayenera kutero, ndipo malinga ndi qawl ina, iye sadzayenera kutero. Mwinamwake, nkhaniyi iyenera kuwonedwa pambuyo pa nkhani yotchedwa 'tertib'.

Tiyerekeze kuti munthu ali ndi bulu wake, wanyamula madzi ndipo bulu wakeyo wasowa; munthuyo pa (nthawi ya Swala akufunika kuchita udhu) ndipo achita tayammum ndi kuchita namaz yake. Akuchita Namaz, udhu wake umaduka ngati amva kulira kwa bulu wake.

Tiyerekeze kuti munthu akuyenda pa hatchi, ndipo anzake sakumudikira kuti atsike pa hatchi yake; Iye achite tayammum pa hatchi pomwepo ndi kuchita namaz mundondomeko yomwe imatchedwa ima, (kutanthauza kufananiza pongochita zizindikiro).

Ngati munthu akuyenda ulendo woopsa m'nyengo yozizira, moti kuchita ghusl kungamudwalitse, nthawi ya namaz ikakwana, iye achite tayammum.

Munthu amene akupita ku ulendo ayenera kukhala ndi duka kapena njerwa mu katundu wake; kuchitira kuti akadzafuna kuchita tayammum pamalo pomwe zinthu zomuzungulira zili zonyowa, ndiye kuti adzagwiritsa ntchito njerwa (kapena duka) pochita tayammum ndikuswali namaz.

Tiyerekeze kuti munthu wayamba kuswali namaz ya Eid ndipo mwanjira ina udhu wake waduka mu nthawi ya namaz; iye achite tayammum ndikupitiriza nawo namaz yake ngati akudziwa kuti kukafuna madzi kumuchedwetsa kubwelera pa Namaz ya Eid, kapena akuopa kuti angatsekerezedwe m'gulu la anthu, apange tayammum ndikuyambiranso kuchita namaz. Qawl iyi ndi yolingana ndi Imam

Azam Abu Hanifa. Koma molingana ndi qawl ya Imameyn[1] ayenera kuchitanso udhu.

[Ahmad bin Muhammad bin Isma'il mu Tahtawi, polongosola za mu Sherblali yomwe ndi ndemanga yolembedwa ndi Abul-Ikhlas Hasan bin Amar pa bukhu yochedwa Meraq-il-felah, wanena kuti: "Matenda ndi 'udhr,' kumasulira kuti ndi chifukwa chovomerezeka m'Chisilamu chochitira tayammum m'malo udhu. Si udhr kwa munthu wathanzi yemwe akuopa kuchita udhu kuti angadwale. Akatswiri amene ananena kuti ndi kololedwa munthu wathanzi kusiya kusala ndikudzachita qada ngati akuopa kuti angadwale atasala kudya m'mwezi wodalitsika wa Ramadan, akunenanso kuti ndi kololedwa kwa munthu wathanzi kuchita tayammum ngati akuopa kuti angadwale atachita udhu ndi madzi.

Zinthu zinayi zomwe zingathe kuchititsa 'kudwala': Madzi atha kukhala chiopsezo ku umoyo wa munthu. Kuyandetsa ziwalo kungakhale chiopsezo. Munthu atha kusatha kugwiritsa ntchito madzi. Mwinanso wina sangathe kuchita tayammum. Ziwopsezozi angazidziwe ndi munthu mwini malinga ndi momwe akudzimvera kapena kuchokera ku chenjezo lochokera kwa dokotala yemwe ndi msilamu wa adil ndi kadaulo pa ntchito yake. Ngati dokotala wa Chisilamu yemwe ndi adil kulibe, chiganizo choperekedwa ndi dokotala yemwe kuchimwa kwake sikumadziwika poyera ndi kwa aliyense chidzakhala chovomerezeka. Munthu yemwe sangathe kugwiritsa ntchito madzi payekha amachita tayammum ngati sangapeze womuthandiza kuchita udhu. Ngati ali ndi ana kapena antchito kapena wina womuthandiza kuchita udhu ngati mnzake, m'modzi mwa anthuwa amuthandize kuchita udhu. Ngati palibe, ndiye kuti achite tayammum. Malinga ndi Imam Azam, ndikosafunika kulemba wa ganyu womulupira kuti amuthandize. Ngati munthu sangathe kuchita tayammum, asiye namaz ndikudzapanga qada atachira. Ngakhale kuti mwamuna ndi mkazi sakufunikira kuthandizana kuchita udhu kapena namaz, mwamuna apemphe mkazi wake kuti amuthandize. Tiyerekeze kuti munthu ali kunja kwa tawuni kapena mudzi ndipo sangapeze madzi otentha; achite tayammum ngati akuwopa kuti akhoza kudwala atachita ghusl ndi madzi ozizira. Fatwa yaperekedwa kuti lamuloli limagwiranso ntchito m'matauni.

[1] Imam Abu Yusuf ndi Imam Muhammad Shaybani, ophunzira awiri akuluakulu a Imam A'zam Abu Hanifa.

Ngati ziwalo zoposa theka l ziwalo za munthu zofunika udhu kapena ghusl ziri ndi zilonda, munthuyo achite tayammum (m'malo mosamba kapena kuchita ghusl). Ngati zilonda ziri malo oposa theka la ziwalo chofuna udhu kapena ghusl, ndiye kuti asambitse malo abwinowo ndi kuchita masah pa zirondazo; ngati masah ingayambitse mavuto ndiye kuti achite masah pa mwamba pa mabandeji. Koma ngati izi zingazetse ululu, ndiye asachitenso masah. Ngati ali ndi chilonda pa mutu pake, moti kuchita masah kungadzetse mavuto, ndiye kuti ndi wololedwa kusachita masah. Tiyerekeze kuti munthu ali ndi mabala m'malo amene ali fardh kusambitsa pochita udhu ku manja onse awiri, komanso nkhope yake ili ndi zilonda; ndiye kuti munthuyo sadzatha kuchita tayammum; choncho amachita namaz popanda udhu. Namaz yake idzakhala yovomerezeka ndipo sadzayeneranso kupempheranso namaz imeneyo. Ngati nkhope yake ili yathanzi, iye asambitse nkhope yake. Ngati alibe womuthandiza amapaka nkhope yake (modekha) pa nthaka. Ngati dzanja limodzi la munthu wathanzi liri lopunduka, lavulazidwa kapena lodulidwa, agwiritse ntchito dzanja labwinolo pochita udhu. Ngati manja ake onse ali choncho, (wopanda manja) iye asisite nkhope yake pa nthaka. Ngati bandeji, chidutswa cha mtengo, mafuta opaka, pulasitala opaka pa chilonda kapena chotupa kapena pa chiwalo chothyoka sizingachotsedwe, kotero kuti mbali imeneyo ya chiwalo siyingasambitsidwe, kapena kuchita masah, chitani masah pa gawo lalikulu lapamwamba pa chotetezeracho. Chitaninso masah m'malo abwino otsalirawo. Koma ngati kuli kotheka, ndi pofunika kuchotsa bandeji kapena mtengo kapena mafuta odzola kapena pulasitala ndi kuchita masah pamalo ovutawo. Ndi kusambitsa mbali yomwe ili ya bwino ya khungulo. Zinthu izi siziyenera kugwiritsidwa ntchito mutachita udhu; komanso palibe nthawi yake yomalizira kugwiritsa ntchito. Ndi zololedwa kupanga udhu ndi madzi phazi lomwe liri bwino ndi kuchita masah pa bandeji phazi lina lomwe likudwala. Ngati chinthu choyikidwa pa balacho chagwa balalo lisanachire, udhu siumawonongeka. Ndiponso udhu siwudzaonongeka ngati bandeji isinthidwa mutachita kale masah. Ngati mafuta opaka pa bala kapena malo ovulala kapena pa phazi pokhapika sangachotsedwe chifukwa choopa kupweteka, ndiye kuti munthuyo wakhudzidwa ndi vuto lotchedwa 'quandary'. Munthu wotere ayenera kusambitsa mbali yakunja kwa mafutawo. Ngati kusambitsa kuli kovuta, ndiye kuti achitepo masah. Ngati masah ingakhalenso yovuta, ndiye kuti asachitenso masah. [Popeza lamulo lomweli likugwiranso ntchito m'Madhhab ena atatu aja, ndikosafunika kutsanzira Madhhab ena.] Zoti mafuta amenewa ali ngati chitetezo zalembedwa m'buku

lotchedwa Ibni Abidin. Koma kumata mano kapena kuvala karauni ndi nkhani yosiyana kwambiri. Poti ndikotheka kutsanzira Madhhab a Maliki kapena Shafi'i.

Ngati munthu asiya kudzizindikira m'maganizo kapena kukomoka osati mozichititsa yekha, ndipo ndikukhala ali choncho mpaka kudutsa nthawi ya ma namaz asanu ndi imodzi, akatsitsimuka sayenera kuchita qada ma Namaz omwe sanachitewo. Iye sayenera kuchita qada. Mosawerengera kuchuluka kwa namaz zomwe munthuyo sanachite ali mu 'ima' (zizindikiro, zofananiza), sakuyenera kuwonjezera ku chifuniro chake (will) kuti isqat ya izo ichitike. Amachita qada ya onse ngati atachira."

Ibni Abidin "rahmatullâhi 'alaih"akunena: "Ndi makruh kwa munthu wathanzi kusambitsira kapena kuchitidwa masah ziwalo zake zofunika kuchita udhu ndi munthu wina. Ndikuloledwa kwa munthu wina kumubweretsera madzi kapena kumuthira madzi pomwe akuchita udhu. Ngati munthu wodwala adetsa zovala zake kapena bedi lake nthawi zonse, kapena ngati kusintha kuli kolemetsa, iye amachita ma namaz ake ndi zovala zake za najszo. Ngati zidutswa za matabwa, plasitala, mafuta odzola zingagwe bala litapola, zifukwa zomulola kuti asachite udhu zitheratu. Ngati bala litapola ndipo mbande zake sizikugwa koma zikhonza kuchotsedwa popanda vuto kapena kumva kupweteka, zifukwa zololeza kuti asachite udhu kapena ghusl zimatha.

Allahu ta'âlâ amadzetsa zowawa ndi matenda kwa akapolo Ake okondedwa kuti awakhululukire machimo awo kapena kuwaonjezera madalitso amene adzapatsidwa ku Mparadiso.

Akapolo Akewo amavutika kumulambira ndipo amatopa. Pofuna kuwabwezera zimenezo, IYE amafewetsera ndikuwapatsa thandizo pa zochita zawo za pa dziko lapansi Amapereka baraka mu rizq lawo (chakudya, zakumwa, ndi zinthu zofunika kwambiri zomwe Allahu ta'âlâ anazikonza kale losatha kuwerengeka ndi kumusungira aliyense mwa akapolo Ake.) IYE sapereka safewetsera kapena kupereka Baraka kwa anthu onyalanyaza mukulambira kwawo mofanana ndi olambira. Anthu onyalanyaza mukulambira kwawo amapeza ndalama pogwira ntchito yotopetsa, mwachinyengo, ndi mwachiwembu. Iwo amakhala ndi moyo wosangalala, wotayilira koma moyo wosakhalitsa konse. Mapeto ake amakathera ku zipatala ndi kundende, komwe amakakhala movutika ndi mwachisoni moyo wawo wonse. Chilango chimene adzakumane nacho patsiku lomaliza chidzakhala chachikulu kwambiri.]

ISTINJA, ISTIBRA, ndi ISTINQA

Istinja ndi kusambitsa ndi madzi ziwalo zodziwika kutero (utakodza kapena kunyera). **Istibra** ndi kudikilira, poyendayenda kapena kuchita china chake utamaliza kukodza mpaka mkodzo uthe mchikodzodzo (usanachite udhu). **Istinqa** ikutanthauza kutsimikiza kwa mumtima za ukhondo wa pathupi.

Pali mitundu isanu ndi umodzi (6) ya Istinja.

Yomwe ili Fardh; Ngati pali najisi yochuluka kuposa kulemera kwa dirham imodzi pa chovala cha munthu kapena pa thupi lake kapena pamalo pomwe amachitira Swalah, ndi fardh kuchotsa najisi ndi madzi. Istinja ili fardh pochita ghusl. [Kulemera kwa Dirham imodzi ndi kofanana ndi kulemera kwa mithqal imodzi yomwe kulemera kwake ndi 4.8 grams.]

Istinja ya Wajib; Ngati pali najisi yolemera ngati dirham (4.8 grams) pa chovala cha munthu kapena pamalo ochitira namaz, zili wajib kuyichotsa.

Ngati najisi ili yopepuka yosakwana 4.8 grams ndi Sunnah kuyichotsa.

Ngati najisi ili yochepa kwambiri zizakhala mustahab kuyichotsa.

Ndipo imakhala Mandub kutsukako ngati munthu watulutsa mpweya ndipo kotulukira mpweyako kwachita chinyezi.

Sunnah za Istinja: Ndi Sunnah kugwiritsa ntchito mwala, dothi kapena pepala lofewa kenako ndi kutsuka ndi madzi mbali yoyeretsedwayo.

Ngati najisi singachotsedwe kwathunthu ndipo yotsalayo ikulemera kuposa 4.8 grams, ndipo ngati najisiyo yapakika kuzungulira kotulukira chimbudzi, ndi fardh kutsukako ndi madzi. Kenako ndikuumitsa ndi nsalu ya ukhondo, kapena ndi dzanja ngati palibe nsalu.

Pali mchitidwe umodzi wokha womwe ndi mustahab pochita istinja: Pomwe mukugwiritsa ntchito miyala, chiwerengero cha miyala chizikhala itatu, isanu kapena isanu ndi iwiri. Osati iwiri, inayi kapena isanu ndi umodzi.

[Munthu amene akudwala matenda osata kuyimitsa mkodzo ayenera kupeza kansalu ka 12 x12 cm. Amange chingwe chachitali theka la metre pa ngodya imodzi ya kansaluko. Msonga ya chida cha abambo ikukulungidwe ndi kansaluko ndipo chingwe chimangidwe kumapeto kwa kansalu, mozungulira chidacho kamodzi. Mbali ya

pafupi ndi kansaluko imakulugidwa kawiri, ndipo kumapeto kopilingizako kudutsa pansi pa kansaluko ndi kukoka kuti chilimbe. Mbali yotsalirayo kumangidwe mfundo yosavuta kumasula, yomwe imangidwe ndi pinifolo ku kabudula wa mkati. Pofuna kukodza masulani pinifolo wotetezerayo, masulanu mfundo ndipo kansaluko kamasulidwe pokoka chingwecho. Ngati zikuvuta kumasula, ndiye kuti pinifoloyo amangiriridwe ku paper clip (wire wopanira ma pepala). Azibambo otere aziyika Chida chawo ndi mipira yawo m'kathumba ka nayiloni ndi kumanga kukamwa kwa kathumbako. Munthu wotsatira Madhhab a Hanafi yemwe ali ndi vuto la kukodza mosayembekezera koma alibe udhr adzachita niyyah yake potsanzira Madhhab a Maliki pamene akuyamba udhu kapena ghusl ndi pochita Namaz. Zanenedwa m'buku lotchedwa **Kitabul-fiqh 'ala-l-madhahib-il-erba'a** lomwe linakonzedwa ndi akatswiri a Chisilamu aku Egypt motsogozedwa ndi 'Abd-ur-Rahman Jeziri "rahmatullâhi 'alaih" (d. 1384 AH), yemwe anali mmodzi mwa mapulofesa a Jami'ul-azhar:

"Malinga ndi qawl ya chiwiri mu Madhhab a Maliki, munthu wodwala kapena wokalamba akakhala ndi vuto lotchedwa haraj (lomwe limawonongetsa) udhu wake, amakhala munthu wa udhr, zomwe zimachititsa iye kukhala okhululukidwa pa udhu wake. Asilamu otsatira Madhhab a Hanafi ndi Shafi'i omwe ali ndi vuto la haraj ayenera kutsanzira qawl (ijtihad) imeneyi." [Msilamu wotsatira Hanafi yemwe amatulutsa mkodzo mosakhala mwachifuniro chake nthawi ya Namaz adzatsatira qawl iyi ya Madhhab a Maliki pamene zinthu sizikuyenda bwino. Iye adzachita niyyah yake ndi kupitiriza namaz yake monga munthu wokhala ndi udhr.]

KACHITA SWALAH

Mu Swalah (Swalah) timalowa m'njira zinayi: Mu (njira ya) fardh; ya wajib; ya Sunnah; ya mustahab. Kukweza manja anu mmwamba kufikira mu mlingo wa makutu anu ndi Sunnah m'Madhhab a Hanafi ndipo ndi sunnah kutembenuzira manja anu ku Qibla. Ndi mustahab, kwa amuna kukhudza makutu awo ndi zala zazikulu, ndikoma akazi akweze manja awo mmwamba malire mulingo wa mapewa awo. Ndi fardh kunena kuti: **"Allahu Akbar".** Ndi Sunnah kugwiranitsa manja anu mukanena 'Allahu Akbar'. Ndi Sunnah kuyika dzanja lanu la manja pamwamba pa dzanja la manzere. Ndi Sunnah kwa amuna kuyika manja awo kunsi kwa mchombo, ndipo kwa akazi kuika pa chifuwa. Ndi mustahab kwa amuna kuti dzanja lawo la manja ligwire pakata dzanja ndi mkono wa manzere. Ndi sunnah pa nthawi ya Swalah kwa

imam ndi omutsatira yemwe, komanso kwa munthu wochita Swalah pa yekha, kunena pemphero lotchedwa 'Subhanaka'.

(Mukanena Subhanaka) ndi Sunnah kunena mawu awa: **"A'udhu billah-im-in-ash-shaytanir-rajim,"** zomwe zimanenedwa ndi imam wotsogolera Swalah (mu Swalah pa jama'at). Munthu wochita Swalah payekha ayenera kunenanso chimodzimodzi koma munthu wotsatira imam mu Swalah ya jama'at asanene izi.

Ndi Sunnah kunena Bismillah (mutanena "Audhu ...). Ndi wajib kunena Fatiha-i-sharifa (Surah yoyamba ya Qur'an al-kareem); ndi fardh kunena (kusoma) ma ayah atatu kapena ayath yaitali yolingana kutalika ngati ma ayah atatu mutamaliza ku soma Fatiha; Ndi fardh kusoma ayah yochokera m'Qur'an al-kareem mukayima m'maraka onse a Swalah omwe ali a Sunnah ndi onse a Witr. Pomwe mukuchita Swalah pa nokha, somani ayah yochokera mu Qur'an al-kareem mukayima m'maraka awiri oyamba a Swalah ya fardh (omwe amakhala ndi ma rak'at anayi).

Ndi fardh kuwelama (popinda thupi) kuchokera m'chiuno pa ruku; Ndi wajib kukhala chiweramire kwa kanthawi uku mukunena kuti, **"Subhanallah"** katatu koma ndi Sunnah kunena kuti, **"Subhana Rabb-iy-al 'adhim."** katatu (nthawi yomwe muli pa Ruku). Ndi mustahab kunena pemphero limeneli kasanu kapena kasanu ndi kawiri. Pakati pa ma sajda awiri, khalani, osasunthasuntha kwa nthawi yayitali yomwe mungathe kunena kuti, **"Subhanallahu,"** kamodzi. Izi ndi fardh molingana ndi Imam Abu Yusuf; koma ndi wajib malinga ndi Tarafayn, (omwe ndi Imam Azam Abu Hanifa ndi wophunzira wake wodalitsika Imam Muhammad.) Ngakhale zili Sunnah malinga ndi akatswiri ena, koma zoti ndi wajib ndi qawl yomwe ili yokhazikika. Pa sajda, ndi fardh kugundutsa mutu pansi kapena tinene kuti pa mswala. Nd ki wajib kukhala choncho kwa kanthawi ndi kunena kuti: **"Subhanallahu"** katatu. Ndi Sunnah kunena kuti, **"Subhana Rabbiy-al-a'la,"** katatu, ndipo ndi mustahab kunena kasanu kapena kasanu ndi kawiri.

Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ" wanena: "Pochita sajda, yambani kugunditsa pansi mawondo anu awiri, kenako manja anu awiri, kenako mphuno yanu ndipo malizirani ndi chipumi chanu. Zala zanu zazikulu za mmanja ndi makutu anu ziyenera kukhala mumzere umodzi. M'Madhhab a Shafi'i manja ayenera kukhala mumzere ndi mapewa. Ndi fardh kuti chala cha kuphazi chimodzi chigunde pansi (kapena pa mswala). Popemphelera payenera kukhala polimbako kuti mutu usalowe mkati. Ikhoza kukhala kapeti, mkeka kapena china chilichonse chomwe mwayala pansi. Tebulo, sofa, kapena

chonyamuka chomwe chayikidwa pansi ndi chimakhala ngati nthaka. Katungwe, pamwamba pa litaka la nsalu, pamwamba pa kapeti yopinda kapena pa chilichonse cholendewera sizingalowe mmalo mwa nthaka. Sajda yochitika pa zinthu za udzu monga mpunga, mapira ndi zina zotero siyidzakhala sahih.

Zidzakhala Sahih ngati zili mu chisaka. Ngati kukwera kwa malo a sajda kuli theka la zra, kutanthauza kuti mulifupi mwake muli zala khumi ndi ziwiri (almost 25 cm) ku kwera kuposa malo amene mwayika maondo anu, Swalah yanu idzakhala sahih; koma zidzakhalabe Makruh. Pa nthawi ya sajda, zigongono zanu ziyenera kukhala zotalikirana ndi thupi lanu, ndipo ntchafu zanu zizikhala zotalikirana ndi pakati pa thuphi lanu. Zala zanu za kuphazi ziyenera kuloza ku Qibla. Ndi Sunnah kuti mafupa a zidendene zanu agundane pamene mukuwelama thupi lanu pa ruku, zigundanenso pa sajda.

Mkazi akamayamba kuchita Swalah, akweze manja ake kufikira cha mmapewa ake. Manja ake asakhale kunja kwa chovala chake. Ayike manja ake pachifuwa pake, chikhatho chake cha ku manja chikhale pa mwamba pa dzanja lake la manzere. Amawelama pang'ono pochita ruku koma chiuno chake chisakhale mzere umodzi ndi mutu wake. Asatambasule dzala za manja pochita ruku ngakhale pa ma sajda onse awiri. Dzalazo zigundane ndipo ayike manja awo pa mawondo awo, omwenso ayenera kupindidwa. Asatsamire kwambiri pa maondo awo. Pochita sajda, agoneke manja awo pansi, zigongono zawo zikhale pafupi ndi mimba yawo. Mimba yawo iyenera kukhudzana ndi ntchafu zawo. Akamakhala pa ‘tashahhud’ (pamene akukhalapochokera pa sajida) akhale ndi mapazi awo atatembenuzira ku manja kwawo. Zala zao ziyenera kuloza ku mawondo awo. [Azibambo asakanikize manja awo ndikugwiritsitsa mawondo awo pomwe akakhala pa tashahhud.] Zala za mkazi zikhale zotsekedwa komanso zigundane. Ndi makruh kwa akazi kuchita Swalah pa jama’at pa iwo okha, kapena kulowerera amuna pamene iwo akuchita Swalah pa jama’at. Si fardh kwa iwo kuchita Swala ya Jumu’ah kapena Swalah ya Eid. (Allahu ta’âlâ sanawalamule kuti azipemphera mapemphero awiriwa).

Amanena **Takbir-i-tashriq** mwakachetechete pambuyo pa Swalah za fardh nthawi yonse ya Eid ya Qurban. Si mustahab kwa akazi kuswali Swalah ya m’mawa ku mmawa kwambiri. Akamachita Swalah asakweze mau ponena mapemphero a mu Swalah. Apa tikumalizitsa kumasulira kwathu kuchokera kwa Ibni Abidin. Sayyid Ahmad Hamawi bin Muhammad Mekki “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih” (d. 1098 [1686 AD]) akufotokoza m'buku lake lotchedwa **Uyun-ul-besair**, lomwe ndi

ndemanga ya bukhu lotchedwa **Eshbah** lomwe linalembedwa ndi Zey-al-'abidin bin Ibrahim ibni Nujaym-i-Misri “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih”, 926 AD - 970 [1562 AD], Egypt:) motere: Kuti ndi makruh tahrimi kwa akazi kumeta tsitsi m’mutu mwawo kapena kulidula kapena kugwiritsa ntchito mankhwala. [Choncho, sikololedwa kwa iwo kufupikitsa tsitsi lawo kuti likhale mulingo wa makutu, malinga ngati asaoneke ngati amuna.]

Ndi makruh kwa mkazi kuchita Adhan kapena Iqamah. Mkazi sangayende ulendo wautali wotchedwa safar popanda mwamuna wake kapena mmodzi mwa achibale ake akuchimuna (mahram). Asaonetse mutu wake pa nthawi ya Haji. Pa nthawi ya Hajj, amachita nawo gawo la mapempemphero lotchedwa Sa’y pakati pa mapiri a Safa ndi Mar’wa ngakhale atakhala mu nsambo. Amachita Tawaf patali ndi Kaaba. Mkazi asachite Khutba. Ziri sahih kuti mawu a mkazi ndi awrat (maliseche). Akhonza kuvala zonyezimira pa nthawi ya Haji. Mkazi ayende nawo anthu omwe anyamula janaza kupita ku manda. Mkazi asaphedwe ngati atakhala murtadd (wampatuko). Pa milandu ya zilango zotchedwa hadd kapena qisas, mkazi saloledwa kukhala mboni. Mkazi asachite i'tikaf mu mzikiti. Ndi zololedwa kwa azimayi kupaka henna mmanja ndi mmapazi awo. [Asagwiritse ntchito polish mzikhadabo.] Akazi awiri amafanana ndi mamuna mmodzi pankhani monga za kulandira kwa chuma chosiyidwa, kuchitira umboni, ndi kupereka nafaqa kwa achibale osauka. Mkazi wa muhsina sayitanidwa kukhoti la milandu. Woweruza kapena wa chiwiri wake amapita kunyumba kwake. (Mkazi wa muhsina, kapena muhsana ndi amene ali wokwatiwa ndi wodzisunga.) Mtsikana asapereke moni kwa mamuna yemwe sali mahram kwa iye kapena kupereka chitonthozo kwa namfedwa wa mamuna yemwe Sali mahram kwa iye. Asanena chilichonse kwa amene akuyetsemula (kunena kuti, “Al-hamd-u-lillah.,”) kapena kuvomereza mawu a mamuna yemwe sali mahram kwa mkaziyo. Asakhale m’chipinda mwayekha ndi mamuna yemwe sali mahram. Apa tikumaliza kumasulira kwathu kuchokera ku Hamawi.

Ndi wajib kukhala pa qa'da-i-ula (kukhala koyamba pochita Swalah), ndipo ndi fardh kukhala pa qa'da-i-akhira, (kukhala komaliza pa swalah). Ndi wajib kunena (pemphero lotchedwa) Tahiyyat pomwe mwakhala kukhala komaliza.

Ndi Sunnah kunena pemphero lotchedwa Salawat mukakhala komaliza kokha pa ma Swalah a fardh ndi pa ma Swalah a wajib. Ndi sunnanso kunena pemphero Salawat pa pemphero la Sunnah

yoyamba ya Swalah ya masana (dhuhr) ndi Sunnah yoyamba ndi yomaliza ya Swalah ya Jumu'ah komanso pomwe mwakhala m'ma Swalah [monga ma rakat anayi asunnah ya pemphero lachiwiri la masana (Asr) ndi Swalahi ya usiku (Esha)] Ndi wajib kunena liwu la salaam, (kunena, '**As-salaamu alaikum wa rahmatullah'**,) ndikutembenuza mutu wanu ku manja kenako ku mamzere ndipo ndi Sunnah kutero. Ndipo ndi mustahab kuyang'ana modzichepetsa.

Kuvomerezeka kwa Swalah yanu kuti ndi yabwino kumatengera inu eni popewa za haram ndi khushu (kuzichepetsandi kuwopa Allahu ta'âlâ) ndi taqwa (kuteteza ziwalo zisanu ndi zinayi ku za haram ndi makruh) ndi kusiya malaya'ni (kupewa zokamba zomwe sizingabweretse phindu pa dziko lapansi kapena pa tsiku lomaliza) ndi tark-i-kasal (kupewa mphwayi pakusunga zomwe zikuchitika mkati mwa Swalah) ndi 'ibdad (kusiya chilichonse chimene mwakhala mukuchita ndi kuthamangira jamaat pamene mwamva kuti Adhan-i-Muhammadi ikuitana, ndi kutero nthawi zonse).

Pali zinthu zisanu ndi chimodzi zofunika kusungidwa pa nthawi ya Swalah: ikhlas; tafakkur; khawf; raja; ru'yat-i-taqsir, ndi mujahada.

Ikhlas imatanthauza kukhala khulus (kukhulupirika) pochita chinthu. [Swalah ichitike pofuna chisomo cha Allahu subhânahu wa ta'âlâ chokha]; tefekkur ikutanthauza kuganiza zinthu mkati mwa Swalah; khawf imatanthauza kuopa Allahu adhîm-ush-shân; raja ikutanthauza kukhala ndi chiyembekezo chopeza chifundo cha Allahu ta'âlâ; ru'yat-i-taqsir imatanthauza kuzidziwa wekha kuti siuli oyera; mujahada ikutanthauza kulimbana pakati pa zofuna za mtima wako ndi zofuna za Satana.

Mukamva kuyitana kwa Adhan-i-Muhammad, muyenera kuganizira za Israfil "alaihim-salâm" akuliza Sur (lipenga la tsiku lachiweruzo); mukuyima ndi cholinga chochita udhu muyenera kudziona ngati mukutuluka mmanda mwanu. Pamene mukupita ku mzikiti muyenera kuganizira ngati mukupita kumalo a Mahsher (msonkhano wa chiweruzo); Pamene muazzin akachita Iqamah ndipo jamaat ikuyambika mutayima m'mizere, muyenera kulingalira mizere ya Asilamu ngati mizere zana limodzi ndi makumi awiri (120) ya anthu pa malo a Mahsher; mizere makumi asanu ndi atatu (80) mwa mizere imeneyi ndi ya Ummat wa Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" ndipo makumi anayi mwa iyo ndi ya Ummat wa Atumiki ena; Mukayima pa swala kutsatira Imam ndipo iye akaymba kusoma Fatiha-i-sharifa, muyenera kudzifanizira ngati muli pa malo omwe Mparadiso uli ku dzanja lanu la kumanja ndipo Jahannama ili ku manzere kwanu;

Azrail „alaihim-salâm” (Mngelo wa imfa) ali pafupi pa mbuyo panu ndipo kuti Baytullah (nyumba ya Allah) mwagundana nayo ndipo manda anu ali pa tsogolo panu ndipo mlato wa Sirat uli pansi pa mapazi anu. Dzifunsani ngati kuyankha kwa mafunso kwanu pa malo a Mahsher kudzakhala kosavuta, ngati mapemphero anu kukhala chisoti cha ufumu pa mutu panu, kukhala bwenzi lanu la pa ulendo wanu wopita ku Tsiku Lomaliza, ndi kukhala muuni wa m'manda mwanu, kapena kuti kudzaponyeredwa m’mano mwanu ngati nsanza yakalekale.

Zopeza za dziko la pansi ndi zosakhulupirika. Ndipo ndi inu ndi otsika!

Namondwe wa imfa aononga zones zimene mupereka mdzina la ulemerero.

ADHAN-I-MUHAMMADI

Ndime ili m'munsiyi yamasulidwa kuchokera m'bukhu lotchedwa **Durr-ul-mukhtar** ndi ndemanga yake ya mutu wakuti **Ibni Abidin:**

Kasomedwe ka mawu ena ophunzitsidwa m'mabuku ophunzitsa zochitika mu Chisilamu zomwe zimachitaka ndi Msilamu wa nzeru zimatchedwa **Adhan-i-Muhammadi**. Munthu wochita Adhan ayenera kukwera pa minaret ndi kunena mawu achiarabu atayimilira. Siyidzakhala Adhan ngati yanenedwa potanthauzira m'zinenero zina ngakhale matanthauzo ake ali olondola. Adhan imachitidwa ndi cholinga cholengeza za nthawi za mapemphero asanu a pa tsiku otchedwa Swalah kapena Swalah. Ndi Sunnah muakkad kwa amuna kuyima malo okwera kunja kwa mzikiti ndi kuchita Adhan. Ndi makruh kwa akazi kuchita Adhan kapena Iqamah chifukwa ndi haram kwa mkazi kulola anthu omwe ndi na-mahram kumva mawu awo.

Muazzin, (munthu wochita Adhan), amayenera kuyima pa malo okwera kunja kwa mzikiti ndi kuyitana Adhan mokweza kuti anthu oyandikana nawo amve. Nkosaloledwa kwa iye kufuula mokweza kwambiri. Akanena, “….**Akbar**,” apume kaye kumapeto kwake zomwe zimatchedwa jazm kapena kupitiriza potchula (vawelo ya chiarabu yosonyeza ‘a’ yotchedwa) ustun. Asatchule vawelo ya chiarabu yosonyeza ‘u’ ndi omwe amatchedwa) oetra. Si halal kuwonjezera mavawelo kapena mawu potalikitsa kayitanidwe koposa mlingo wake wokhazikika wa mawu kapena kuyiwononga kukhala nyimbo, ndi machitidwe ena opeka. Ndi Sunnah kutembenuza mutu ku manja ndi

ku manzere pamene mawu oti '….salah' ndi '..falah' akunenedwa koma mapazi ndi chifuwa zisatembenuke nawo.

Ziyang'anebe ku Qibla. Adhan imakhoza kuyitanidwira kuchokera mu minaret; ndipo pa nthawiyi muazzin amatembenuka malo ozungulira minaret. Minaret yoyambilira kwambiri inamangidwa molamulidwa ndi Hadrat Mu'awiya "radiyallâhu anh"mu 19 B.H. – 60 [680 A.D.]). Panali nsanja yomwe inamangidwa pa msikiti wa Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam". Billal Habashi "radiyallâhu anh"(d. 20 A.H. Damascus) amakwerapo ndi kuchita Adhan. Rasulullah sall-Allahu 'alaihi wa sallam adalamula Bilal kuti ayike zala zake m'makutu mwake pochita Adhan. Adhan izabwerezedwa ngati wachitayo walankhula akuchita Adhan. Wochita adhan akayankhula akuchita adhan, adhanayo iyenera kubwerezedwa. Ndi zololedwa kuti anthu oposa mmodzi kuchita Adhan pa modzi. Adhan, siyidzakhala sahih ngati akusiyana mau onena. Ndi makruh tahrimi kuchita Adhan atakhala. Zili Sunnah kwa Muazzin kukhala Msilamu wa Salih, wodziwa zochita za Sunnah mkati mwa Adhan ndi nthawi yochita Adhan. Ndi Sunnah kuchita Adhan tsiku lililonse mokhazikika ndi mosalekeza. Ndi Sunnah kuchita Adhan chifukwa cha chisomo cha Allahu subhânahu wa ta'âlâ osati pofuna malipiro apa dziko lapansi). Koma nkololedwa kumulipira Muazzin kangachepe ndipo iye avomere kulipidwako. Adhan yochitika ndi mwana wosakhwima mmaganizo siyidzakhala sahih. Pakuti, mawu ake ndi ofanana ndi kuyimba kwa mbalame kapena phokoso lopangidwa ndi chida choyimbira. [Pa chifukwa ichi, Adhan kapena Iqamah yochitidwa pogwiritsa ntchito zokuzira mawu sizikhala sahih. Adhan yochitika ndi fasiq (munthu wopwanya malamulo a chisilamu) njosavomerezeka. Nawo ma takbir omwe imam angachite pa Swalah imene jamaah yake yayimitsidwa ndi fasiq sadzavomerezedwa. Ndi makruh kwa iye kuchita Adhan. Ndikofunikira kuti muazzin adziwe kuti amachita Adhan mu nthawi yoyikidwa ndi cholinga choti Asilamu ena adziwe ndi kuti akachite Swalah mu nthawi yake yokhazikitsidwa. Munthu akayamba kuchita Swalah asakudziwa ngati nthawi yake yakwana, Swalah wachitayo siyidzakhala sahih, ngakhale zitadzakhazika kuti wayichita mkati mwa nthawi yake. Swalah yochitika motsatira kalendala yokonzedwa ndi osakhulupilira kapena ndi ma fasiq siyidzakhala sahih. Pa zogwiritsa ntchito kalendala yolondola ku Dar-ul-harb (dziko la Asilamu), munthu uyenera kufunsa Msilamu yemwe ukukhulupilira kuti ndi Salih komanso ophunzira ndi kumvwa chowonadi kuchokera kwa iye.] Tiyerekeze kuti ma adhan angapo akuchitika mogwirizana ndi Sunnah nthawi imodzi m'malo angapo ndipo onse ukuwamva; muyenera kubwereza potsatira Adhan

yoyamba kuyimvayo. Ndipo ngati ikuchokera ku mzikiti womwe mwakhala mukupemphera tsiku ndi tsiku, mupite kumeneko kukachita jama'at.

Muyenera kubwereza pambuyo pa Adhan ngakhale mukuwerenga kapena kunena pa mtima Qur'an al-kareem. Mu nthawi iazi, simuyenera kubwereza Adhan; ngati mukuchita Swalah mu jama'at, muli mchimbudzi, mukudya, muli mu mzikiti, mukuphunzitsa kapena kuphunzira chidziwitso cha chipembedzo. Kuchita Adhan m'chinenero china osati Chiarabu kapena m'njira yokhla ngati mukuyimba nyimbo ndi kuphwanya Sunnah. Ndi mustahab kwa munthu kuti akamva Adhan ayimirire ngati wakhala ndi asiye kuyenda ngati akuyenda. Zikunenedwa motere polongosola za malonjezo pa nkhani ya kulumbira: "Ndi wajib kuti boma la Asilamu limange msikiti m'gawo lililonse la dziko. Misikiti imamangidwa ndi ndalama zochokera ku Bayt-ul-mal (nyumba ya zachuma). Ndi wajib kuti Asilamu adzimangire mzikiti ngati boma silimamanga.

Monga zikuonekera, ngati Chisilamu chikumveredwa ndipo mzikiti wamangidwa m'dela lirilonse la mzinda, Adhan idzachitika mmalo onse a mu zinadwo ndipo aliyense adzamva kuyitana kwa Adhan m'dera lake. Sipadzafunikanso kuti muazzin azifuula mokweza kwambiri kapena kugwiritsa ntchito zokuzira mawu. Chimkuza mawu ndi bidah yomwe imayambitsa kuphwanya ma Sunnah a Adhan. Zimapangitsa ma Sunnah awa kutha kukongola kwawo. Ichi ndi chifukwa chake ndime ya khumi ndi chisanu (15) ya chigamulo cha 137 cha commission yomwe inapatsidwa mphamvu kukambirana ndi kuphunzira za ntchito za chipembedzo motsatira malamulo otsogolera nkhani za chipembedzo (ku Turkey) zomwe zinasindikizidwa pa 1/12/1954 ikukamba motere: "Kuyika zokweza mawu pa minbar m'misikiti ndikoletsedwa ndithu. Ngati jama'at (kusonkhana kwa Asilamu pochita Swalah pagulu) ndi yaikulu kwambiri moti ma takbir a imam ndi zowerenga zake sizimveka, ndiye kuti m'modzi mwa ma muazzin kapena wina wakumbuyopo atha kutenga udindo wobwerezanso ndi liu lake." Zafotokozedwa mwakuya kwambiri pa mutu wonena za sajda-i-tilawat m'bukhu lotchedwa **al-Fiqh-u-'alal madhahib-ularba'a** komanso chakumapeto kwa mutu wa 16 wa bukhu lachinayi lotchedwa **Endless Bliss** kuti Qur'an al-kareem yowerengedwa kapena kunenedwa kapena Adhan zomveka kuchokera pa wayilesi kapena kuyika pa tepi kapena yochitidwa ndi chimkweza mawu si mawu a munthu; izo ndi mawu omveka kuchokera ku zipangizo za nyesi ndi magetsi zoyendetsedwa ndi yemwe

wazitsekulayo. Izi siziyenera kukhala liwu loyambilira la munthu lomwe limachititsa kuti zipangike. **Adhan-i-Muhammadi** yololedwa ndi Chisilamu iyenera kukhala liwu la Muslim wa Salih. Phokoso lotuluka m'chitoliro si Adhan.

Hamdi Efendi wa Almali "rahima-hullâhu ta'âlâ", m'modzi mwa akatswiri achipembedzo a masiku ano, akunena motere pa tsamba la zana makumi awiri ndi atatu mphambu makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu imodzi (2361) m'bukhu la chitatu la Tafsir: [Monga tawonera, malamulo okhudza 'kumvetsera ndi kukhala chete' apangidwa kukhala oyenera pa qiraat (po lakatula), yomwe ndi ntchito yosankha chinenero poyang'ana malo ovomerezeka ofotokozedwa kuti akugwirizana ndi cholinga cha mawu ndikuti zikumveka. Kunena zoona, ngakhale ntchito anagwira m'ngelo wamkulu Jebrail m'mene Qur'an al-kareem imavumbulutsidwa kwa Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam" zinali zomuchititsa Mtumiki wodalayu kuchita qiraat, osati kuti amachita qiraat payekha. Ntchito yopatulika yochitidwa ndi Allahu ta'âlâ, kumbali ina, inali ntchito ya tenzil (chivumbulutso) ndi kukonza kwa ntchito ya qiraat. Choncho mawu otuluka kuchokera ku chinthu chopanda ubongo sangatchedwe qiraat; komanso mawu omveka otuluka mlengalenga sangakhale qiraat. Chifukwa chake ma Fuqaha, (akatswiri a Chisilamu omwe anazama pa maphunziro mu nthambi ya Chisilamu yotchedwa Fiqh), ananena kuti mau omveka kuchokera ku qiraat yomwe ikuchitika sayenera kutchedwa qiraat. Ndipo ndi kosafunikira kuzitsatira ngati momwe ungachitire utamva qiraat monga kuchita sajda yotchedwa 'tilawat' yomwe ili yoyenera kuchitidwa ndi Msilamu yemwe akuwerenga kapena akunena pa mtima Quran akamva ayah ya sajda. Monga kuwerenga mwakachetechete bukhu lina lililonse sikungakhale qiraat, chimodzimodzi kumvetsera mfuwu wa cholira kapena wopangidwa ndi chida choyimbira chomwe chikuyimba sikumvetsera ntchito za qiraat. Kotero mawu ochokera pa tepilikoda, wayilesi yomvera, wayilesi ya kanema kapena DVD yowonetsa mawu ndi zinthunzi, munthu akuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem, ndi mfuwu wa qiraat osati qiraat payokha. Choncho izi sizingachititse Msilamu kumvetsera ndi kukhala chete kwa Msilamu amene wamva kapena kumvera). M'mawu ena, ma ayah a Qur'an al-kareem momwe ali wajib (okakamizidwa) kuwamvetsera mwakachetechete ndi ma ayah omwe akuwerengedwa kapena kunenedwa pa mtima ndi munthu mwakuchita qiraat, osati ma ayah omvera pa zoyimbira. Komabe, mfundo yakuti kumvera pa zoyimbira siziri wajib kapena mustahab zisachititse munthu kugamuala kuti ndi kosaloledwa kumvera kapena

kuti ndi wajib kusamvera. Pakuti, kusewera ma ayah a mu Qur'an al-kareem pa wayilesi ndi zida zina ndi kumvetsera ma ayah a mu Qur'an al-kareem akuwerengedwa ndi munthu ndi zinthu ziwiri zosiyana. Ndi zowonekeratu kuti si chinthu chovomerezeka kusewera ma ayah a mu Qur'an al-kareem pa wailesi ndi zina zotero kapena kuzifalitsa kudzera mu zipangizo zotere. Ndizachidziwikire kuti ngakhale mchitidwe wa qurbat (kuziyandikitsa) monga kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem ndi wofunika, ndi kulakwa kutero m'malo omwe ndi osalongosoka komanso osayenerana ndi ulemelero womwe umayenera kukhalapo ndi ntchitoyi.

Koma ngati kulakwaku kwachitika ndi anthu ena, kusamvera mmalo momvera kudzakhala kulakwa kwina. Mwachitsanzo, ndi kulakwa kuchita qiraat (kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem) m'malo osambira aliyense. Koma ngati wina achita, simukapeza thawab (malipiro a tsiku Lomaliza) chifukwa choti simunamvere nawo. Chimodzimodzi mutha kunena kuti sikofunika kumvera mawu a qiraat ya Qur'an al-kareem oyimbidwa kapena kuyikidwa pa (chinthu chonga) choyimbira nyimbo kapena kuwulutsidwa pawailesi. Musatanganidwe kupewa kumvera poti ndi zofanana ndi qiraat ngakhale siziri qiraat pa zokha. Ndi zosonyeza Kalam-i-nafsi, (Liu la Allahu ta'âlâ.) Choncho, ngakhale siziri wajib kapena mustahab monga kumvera qiraat yeniyeni, ndi zololedwa komanso ndi zoyamikirika kutero; Ponena zowona palibe chifukwa chokwanira chosalemekezera izi. Mkhalidwe woterewu ukufanana ndi Msilamu amene awona tsamba la Qur'an al-kareem litasiyidwa p amalo osayenera ndi ulemu wake waukulu ndi udindo wake wa chipembedzo politola ndi kuliyika penapake poyenerana ndi chiyero chake, osati kungodutsa osasamala."]

Zalembedwa m'mabuku ambiri a Fiqh, monga mu **Qadikhan:** "Ndi ntchito ya Sunnah kuchita Adhan. Chifukwa ndi limodzi mwa makhalidwe ndi zizindikiro za chipembedzo cha Chisilamu. Ngati anthu okhala mumzinda wina kapena chigawo lina la mzindawo aleka kuchita Adhan, boma liyenera kugwiritsa ntchito mphamvu kuwaumiriza kuyambiranso mchitidwewo. Muazzin, (Msilamu yemwe ntchito yake ndi kuchita Adhan), ayenera kudziwa mbali ya ku Qibla ndi nthawi za Swala zisanu za pa tsiku. Ndithu, ndi Sunnah kuchita Adhan mutayima, nkhope yanu itayang'ana ku Qibla kuyambira pa chiyambi mpaka kumapeto. Adhan imachitika ndi cholinga chodziwitsa anthu nthawi ya Swalah zisanu za pa tsiku ndi nthawi ya iftar, (nthawi yomwe Asilamu akuyenera kumasula kusala.) Zimayambitsa fitna kuti munthu

wosadziwa nthawi zopemphelera kapena yemwe ndi fasiq achite Adhan. Ndi makruh (zonyansa) kuti anthu awa achite Adhan: mwana wosazindikira, munthu woledzera, munthu wosokonekera mmaganizo, munthu wa janab kapena mkazi. Zikatero, Adhan idzayenera kuchitikanso ndi Muazzin wovomerezeka.

[Zimapereka thawab zochuluka kuchita Maulidi, ndi kupita kumalo komwe akuchita Maulidi kukamvera. Koma ndi haram kwa mkazi kuti amuna omwe ali na-mahram kwa iye kuti amve mawu ake pochita Maulidi kapena Adhan. Ndi haram mkazi kuyimba kapena kuyankhula mokweza kwambiri kuposa momwe amafunikira pa maso pa amuna omwe ndi na-mahram kwa iye. Mkazi yemwe akufuna kuchita zopembedza zotere azichita zimenezi pakati pa akazi okha. Asatenge tepi kapena kujambula mawu ake kapena kuwalola kuti aziwulutsidwa kudzera pa wailesi kapena pa wailesi yakanema.] Ndi makruh mamuna kuchita Adhan atakhala pansi kapena ali opanda udhu. Ndi makruh kuchita Adhan utakwera nyama monga kavalo ndi kumazungulira m'mudzi. Koma Adhan imeneyo siyiyenera kubwerezedwa. Adhan iyenera kuchitikira pa minaret kapena paliponse mwa chindunji kunja kwa mzikiti. Isachitike mkati mwa mzikiti. Ndi makruh kuchita Adhan m'njira ya 'talhin', komwe ndi kuyimba mokweza ndi kutalikitsa masilabulo moti mpaka kusokoneza mawu.

Adhan isachitike m'chinenero china chiri chonse kupatula Chiarabu." Zanenedwa m'buku la **Fatawa-i-Hindiyya** kuti: "Ndi makruh kwa muazzin kufuula mokweza mpaka kudzitopetsa (pochita Adhan). **Ibni 'Abidin** "rahima-hullâhu ta'âlâ" akunena kuti: "Zili Sunnah kwa muazzin kuima malo okwera kuti achite Adhan kuti azimveka kutali. Ndi zololedwa kwa ma muazzin oposa mmodzi kuchita Adhan limodzi." Monga momwe zikumvekera m'ndime za ukatswirizi, ndi bid'at kuchita Adhan kapena Iqamah kapena kuchita Swalah ya jama'ah pogwiritsa ntchito zokweza mawu. Ndipo ndi tchimo lalikulu kuchita bidah. Hadith-isharif imati: **"Ngati munthu achita bidah, palibe ntchito iriyonse ya kupembedza kwake yomwe ingakhale yovomerezeka."** Ngakhale kuti liwu lomveka kuchokera m'chimkweza mawu ndi lofanana kwambiri ndi liwu la munthu, ilo siliri liwu la munthu. Ndi mawu opangidwa ndi zidutswa zosunthika ndi maginito. Si mawu a munthu amene wayima pa malo okwerawo. Tchimo laliwonjwzerek akayika chimkweza mawu ku manja kapena ku manzere kapena kumbuyo kwa minaret kapena pa denga, poti mawu samachokera mbali ya Qibla. Sikofunikira kuti mawu apite malo akutali kapena kuti ife tiyime ndi kukuwa ngati chimkweza mawu. Ndi

kofunika kumanga mzikiti dela lirilonse. Potero Adhan idzachitika mbali zonse ndipo gawo limodzi mwa magawo anayi a Adhan lidzamveka kuchokera kumalo okhala onse. Komanso **Adhan-i-jawq** ndi yololedwa. Ma muazzin oposa mmodzi akamachita Adhan nthawi imodzi imatchedwa Adhan-i-jawq.

Mawu okoma a munthu adzamveka kuchokera kutali, kusuntha mitima ndi miyoyo, ndi kutsitsimutsa iman ya anthu. [Muazzin amachita Adhan ndipo imam amachita qiraat ndi mawu awo achilengedwe mokweza molingana kuti amveke kwa Asilamu omwe amuzungulira mzikitiwo ndi omwe ali mu jamaah. Ndi makruh kwa iwo kuyesetsa kuti mawu awo amveke patali. Izi zikusonyeza kusafunikira kogwiritsa ntchito chimkuza mawu.] Mwachidule, liwu lotuluka m'lipenga lotchedwa sipikala si Adhan**. Adhan-i-Muhammadi** ndi mawu otuluka mkamwa mwa muazzin. Hadithi sharif yochokera m'bukhu lotchedwa **Hilya-t-ul-Awliya** lolembedwa ndi katswiri wamkulu wa Chisilamu dzina lake Abu Nuaym Isfahani (Ahmad bin 'Abdullah) "rahmatullâhi 'alaih" (336 [948 AD] - 430 [1039)]) imati: **"Liu la Adhan lomwe limatuluka m'chiwiya choyimbira ndi liwu la Satana. Anthu amene amagwiritsa ntchito zimkweza mawu pochita zimenezo ndi ma muazzin a Satana."**

Zanenedwa motere mu Hadith-i-sharif: **"Pamene tsiku lachimaliziro likuyandikira Qur'an al-kareem idzawerengedwa** (ndi kuyilakatula) **kudzera mu mizmar**. **Idzawerengedwa** (ndi kulakatulidwa) **osati chifukwa cha chisomo cha Allahu ta'âlâ, koma chifukwa cha chisangalalo." "Pali anthu ambiri amene amawerenga Qur'an al-kareem,** koma Qur'an al-kareem **imawatemberera."** "**Idzafika nthawi yomwe ma muazzin adzakhala anthu oyipitsitsa mwa Asilamu." "Idzafika nthawi yomwe Qur'an al-kareem idzawerengedwa kudzera mu mizmar. Allahu ta'âlâ adzawadzudzula anthu ochita zimenezo."** Mizmar imatanthauza mitundu yonse ya zida zoyimbira ndi mapaipi. Chimkuzamawu ndi mizmar. Ma Muazzin ayenera kuopa ma Hadithi sharif awa ndi kupewa kuchita mapemphero awo kudzera m'zoyankhulira. Anthu ena osaphunzira m'chipembedzo amanena kuti choyankhuliracho n'chothandiza chifukwa chimanyamula mawu kumadera akutali. Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Chitani mapemphero monga mukundionera ine ndi ma Sahabah anga tikuchitira! Anthu amene amasintha zochita zopembedza amatchedwa 'ahl-i-bidah'** (anthu a bidah, ochita za bidah). **Anthu a bidah ndithudi adzapita ku Jahannama. Palibe chilichonse mwa mapemphero awo chidzalandiridwa.** Sikolondola kunena kuti, "Tikuwonjezera zinthu

zothandiza pa kulambira.” Mawu ngati amenewa ndi mabodza onenedwa ndi adani achipembedzo. Akatswiri Achisilamu okha ndi amene amadziwa ngati kusintha kudzakhala kothandiza. Akatswiri ozama amatchedwa ma **mujtahid**. Ma mujtahid sangathenso kusintha zinthu paokha. Amadziwa ngati kuwonjezera kapena kusintha kwina kudzakhala bidah. Pali kugwirizana kuti ndi bid'at kuyitana Adhan pogwiritsa ntchito 'mizmar'. Ndi mtima wake wa munthu ungachititse kupeza chisomo ndi chikondi cha Allahu ta’âlâ.

Mtima umabadwa ngati kalilole woyera. Kupembedza kumawonjezera kuyeretsa mtima ndi kuwupukuta. Bidah ndi machimo zimadetsa mtima, kotero kuti sungathenso kulandira fayz ndi nur zobwera ku mtimako mu njira ya chikondi. Asilamu a Salih amatha kulingalira za vuto limeneli ndipo amakhala ndi nkhawa. Safuna kuchimwa. Amafuna kuchita zinthu zambiri zolambira. Kuwonjezera pa kuchita mapemphero asanu a Swalah tsiku lirilonse, amalakalaka kuchita zambiri. Nafs ya munthu imakondwera ndi kuchita machimo; zimamveka ngati ndi zothandiza. Ma bidah onse ndi matchimo zimadyetsara ndi kulimbikitsa nafs za anthu, zomwe ndi mdani wa Allahu ta’âlâ. Chitsanzo cha izi ndi kuyitana Adhan kudzera mu chimkuzamawu. Rauf Ahmad, m'modzi mwa olowa m'malo mwa Abdullah Dahlawi, akunena motere m'mawu ake oyamba ku **Durr-ulma'arif**: "Ndi haram kuwerenga kapena kunena Qur’an al-kareem kapena kuchita ntchito zina pogwiritsa ntchito zida zoyimbira zotchedwa ‘mizmars’.” Chitsanzo ndi kuyitana kwa Adhan kudzera mu chimkuzamawu.

[Zanenedwa motere m'mabuku a Shafi'i otchedwa **al-Muqaddima-t-ul-hadramiyya** lolembendwa ndi Abdullah bin Abd-ur-Rahman) ndi **al-Anwar li-a'mal-il-ebrar** lolembedwa ndi Yusuf Erdebili,) d. 799 AH): “Kuti ikhala sahih m’Madhhab a Shafi’i, kwa Msilamu kuti atsatira imam mu Swalah ya jama’at mu mzikiti, iye ali kunja kwa mzikiti umenewo, zinthu zitatu ziyenera kukwaniritsidwa: 1) Ayenera kukhala pamalo pomatha kumuona imam; 2) Ayenera kumamumva imam; 3) Pasakhale mtunda wa ma dhra atatu (300 x 0.42=126 meters) pakati pake ndi mzere wakumbuyo wa jama’at." Palibe ngakhale m’Madhhab a Hanafi kapena a Shafi’i pomwe Swalah itha kukhala sahih (yovomerezeka) potsatira imam wakutali yemwe akuwonedwa ndi kumveka pa TV. Ndi mchitidwe wa **bidah** kusokoneza mapemphero powaonjezera machitidwe otere omwe kunalibe munthawi ya Salaf-i-Saalihin. Monga zikumvekera kuchokera mu ayah ya zana limodzi ndi chinayi (104) mu Surah Nisa, anthu omwe amachita bid'at pokhazikitsa

zochitika popembedza monga Adhan ndi Swalah pa ma wailesi, ma TV ndi zoyankhula mokweza, adzapita ku Jahannama. Mawu omveka kuchokera m'choyankhulira kapena pa wailesi si Adhan yeniyeni, koma ndi zofanana ndi Adhan. Momwemonso, masomphenya a munthu pa galasi kapena pa chithunzi si munthu yemwe ali iyeyo, koma ndi chinthu chofanana ndithu, ngakhale kuti ali ndi mawonekedwe ake enieni.]

MA WAJIB A SWALAH: Ma wajib a Swalah m' Mu Madhhab a Hanafi, ma wajib ali motere: Osawerenga kalikonse mutanena "Subhanaka..." pamene mukuchita Swalah mu jama'at pambuyo pa imam. Kwa imam yemwe akutsogolera Swalah mu jama'at ndi kwa Msilamu amene akuchita Swalah pa yekha awerenge Surah yotchedwa **Fatiha sharifa** kamodzi pa ma rak'at awiri aliwonse omwe ali fardh ndi pa rakaat iliyonse yamtundu wina uliwonse.

Kunena Surah yowonjezera zomwe zimadziwika kuti **Dhamm-i-Surah** kamodzi pa ma rak'at awiri oyambilira a Swalah yomwe ili fardh ndipo ili ndi ma rak'at anayi kapena atatu komanso pa rak'at iliyonse ya mtundu wa Swalah wina uliyonse. Kugawa Fatiha-i-sharifa mu rakat awiri oyambilira mu Swalah ya ma rakat atatu kapena zinayi. Kudutsa kuchokera ku fardh kupita ku fardh ina. Kuwerenga Fatiha musanawerenge dhamm-i-Surah. Kukhala pa Qa'da-i-ula (kukhala koyamba). Kuchita sajda (kawiri) imodzi pambuyo pa inzake. Kunena pemphero lotchedwa Tahiyyat pa nthawi ya Qa'da-i-akhira (kukhala komaliza). Kumalizitsa Swalah ponena Salaam, -"As-salaam-u'alaikum wa rahmatullah." Kupemphera mapemphero otchedwa Qunut pa Swalat-i-witr. Pakuchita Swalah ya Eid, kunena ma takbir owonjezera. Kunena pemphero lonenedwa nthawi ya Swalah mwa ikhfa', (monong'ona) pomwe payenera kuchita mwa ikhfa', mwa jahr (momveka,) pomwe payenera kuchita mwa jahr. Kutsatira Ta'dil-i-arkan pamene mukuchita Swalah. Uku ndi kukhala kanthawi osasuntha pa malo aliwonse; nthawi yokwanira kunena kuti, "Subhan allahu," pamwe muli pa ruku; nthawi yokwanira pa qawma, pomwe ndi nthawi yoyimilira mukuchokera pa malo a ruku; Nthawi yokwanira pa sajda zonse ziwiri komanso pa nthawi ya jalsa, yomwe ndi nthawi yomwe mukukhala pakati pa sajda awiriwo. Nthawi zokhala osasunthasunthazi zimatchedwa 'tumaninat'.] Kuchita sajda ya Tilawat ngati mwawerenga ayah ya Tilawat nthawi ya Swalah kapena mwamva imam akunena pa Swalah muli pa jama'at. Kumachita sajda-i-sahw ngati ndi kofunika.Mu Swalah za fardh zomwe zili ndi ma rakat anayi, kuyima mwachangu mukangonena pemphero lotchedwa Tahiyyat,

popanda kuchedwa pa Qada-i-ula (kukhala koyamba). Kutsatira imam muzochitika zonse. Malinga ndi qawl, chichita Swalah za fardh mu jama'at pokhapokha ngati muli ndi udhr (chifukwa chovomerezeka ndi chololedwa ndi Chisilamu,) kuti chikulepheretseni kutero.

Pakutha pa Swalah iliyonse ya fardh mwa Swalah 23 omwe mumachita mutamaliza Swalah ya m'mawa wa tsiku la Arafa (tsiku lomwe limatsatiridwa ndi tsiku loyamba) la Eid ya Qur'an mpaka Swalah ya masana pa tsiku la chinayi la Eid ya Qurban, (kuphatikiza pemphero lomaliza,) mukhale mukunena **takbir-i-tashriq.**

SUNNAH ZA SWALAH: Sunnah za Swalah m'Madhhab a Hanafi zili motere: Pa takbir ya iftitah, (takbir yomwe imanenedwa poyamba pa Swalah,) komanso pa takbir ya Qunut, pomwe mukunena kuti, "Allahu akbar," musanayambe kunena pemphero lotchedwa Qunut poyimilira komaliza mu Swalah-i-Witr, amuna akweze manja awo m'mbali mwa makutu awo ndi kuti akazi akweze manja awo kufikira cha mmapewa, ndipo onse (amuna ndi akazi) atembenuzire manja awo ku Qibla kanthawi pang'ono. Panthawi ya Qiyam, (poyimilira mu Swalah,) dzanja lamanzere liyenera kukanikizidwa pogwiritsa ntchito chala chachikulu ndi chala chaching'ono chakumanja. Koma akazi ayike dzanja lawo lakumanja pamwamba pa dzanja lawo lamanzere. Amuna amakanikiza manja awo powayika mmunsi mwa mchombo, ndipo akazi amawayika pachifuwa. Kunena pemphero loti, **"Subhanaka...,**' pa rakat yoyamba ya Swalah iliyonse – kwa imam ndi jama'at komanso opemphera pa yekha achite chimodzimodzi. Imam ndi wochita Swalah pa yekha, anena Audhu ndi Bismilla atanena Subhanaka mu rakat yoyamba. Momwemonso, imam ndi wochita Swalah pa yekha, anene Bismillah-i-sharifa asananene Fatiha-i-sharifa pa rakat iliyonse. Kunena kuti, "Amin", – mwakachetechete kumapeto kwa Fatiha-i-sharifa, zomwe zili zoyenera kwa onse, -imam wotsogolera Swalah mu jama'at ndi Asilamu (gulu lotsatira lotchedwa) jama'at 'amin', anenedwe Imam akangonena kuti, "... **wa la-d-dallin**," omwe ndi mawu awiri omaliza a Surah yoyamba ya Qur'an al-kareem yotchedwa Fatiha. Naye munthu wopemphera pa yekha[1] akamaliza kuwerenga Fatiha anene kuti 'Amin'. Kuchita Takbir, kunena, "Allahu akbar," powerama pa Ruku kuchokera pa Qiyam (poyimilira). Kuyika manja anu, zala zanu mutatambasula pa mawondo anu, pa Ruku. Kunena kuti**, "Subhana Rabb-iy-al 'adhim,"** katatu pa Ruku. Pa Ruku, mutu wanu ndi chiwuno

[1] Ndi wochita pa yekha' tikutanthauza Msilamu wochita Swalah yekha.

chanu ziyenera kukhala zofanana.[1] Imam wotsogolera Swalah mu jama'at ndi kwa wochita pa yekha, kunena, **"Sami'Allahu liman hamidah,"** pamene akuwongoka kuchokera mu Ruku. Kwa Msilamu wochita Swalah mu jama'at kapena pa yekha, kunena kuti, **"Rabbana laka-l-hamd,"** atawongoka kuchokera ku Ruku. Kunena kunena: **"Allahu akbar"** potsikira pa Sajda kuchokera pa qiyam.

Kunena kuti, **"Subhana Rabb-iy-ala'la,"** pa nthawi ya Sajda. Kunena **"Allahu akbar"** pamene mukukweza mutu ndi kukhala kuchokera pa sajda yoyamba. Kunena kuti, **"Allahu akbar,"** potsikira pasajda yachiwiri. Kukumaniza zala pamodzi pa sajda. Pa sajda, amuna ayenera kuyika mawondo awo pansi (kapena pa mkeka) ndikulekanitsa ntchafu zawo ndi mimba zawo; akazi ayenera kugundanitsa ntchafu zawo ndi mimba zawo. Kunena kuti, **"Allahu akbar,"** ponyamuka pa sajda ya chiwiri. Amuna akhalire phazi lawo la ku manzere, ndipo awongole phazi la kumanja. Kunena Swalawat pa Qa'da-i-akhira (pa kukhala komaliza). Kutembenuza mutu wanu kumanja ndi kumanzere pamene mukuchitira salaam. Pa nthawi yokhala pansi pamene mukunena pemphero Tehiyyat, ikani manja anu pa ntchafu zanu. Nsonga za zala zanu zikhale molingana ndi nsonga za mawondo anu ndipo dzala zikhale pazokha. Manja anu ndi zala zanu za kumapazi ziyang'ane ku Qibla pochita Sajda, ndipo manja anu akhale mzere umodzi ndi makutu anu. Kuchita Sajda pogwetsa pansi ziwalo zanu zisanu ndi ziwiri limodzi. Kunena Surah Fatiha sharifa yokha pamwe mayima m'marakat awiri omaliza a Swalah za fardh zomwe ziri ndi ma rakat anayi. Kunena Adhan-i-Muhammadi m'njira yomwe Sunnah-i-sharifa imanenera. Kwa amuna kuchita Iqamah asanayambe Swalah za fardh, akamapemphera pa jama'at ngakhale akupemphera pa okha.

MUSTAHAB A SWALAH: M'Madhhab a Hanafi Mustahab a Swalah ali motere: Kuti jama'at iyime mosazengereza muazzin akangotchula mawu akuti, "Hay-ya-'ala-s-salah," akamachitira Iqamah, yomwe imadzutsa okhulupirira kuti ayambe kuchita Swalah. Kuti amuna agwire nsonga za makutu awo ndi zala zao zazikulu akamanena Takbir ya Iftitah ndi Takbir ya pa mapemphero a Qunut mu Swalah ya Witr. Pa nthawi ya qiyam, kugwira dzanja lamanzere mwamphamvu kwambiri. Pa nthawi ya qiyam, maso awo ayang'ane pa malo a sajda. Pa Ruku ndi pa sajda, kunena tasbih, kuti, **"Rabb-iy-al 'adhim,"** ndi

[1] Ndi zosachita kufunsa kuti ena mwa malamulowa amagwira ntchito kwa amuna okha. Tikulangiza amayi kuti awerenge ndime yomaliza ya mutu wa 14 wa Gawo la chinayi la bukhu la **Endless Bliss** kuti adziwe zambiri za momwe amayi amachitira Swalah.

“Rabb-iy-al-a’la,” mosatizana choncho kasanu kapena kasanu ndi kawiri. Kuyang'ana pa mapazi anu pamene mukuchita Ruku. Kuyandikitsana mapazi anu pamene mukuwerama pa Ruku. Kuchotsa phazi lanu lakumanzere kuchokera ku phazi lanu la kumanja pamene mukuwongoka kubwelera ku (malo) a qiyam.

Kugunditsa mphuno yanu pansi kapena pa mswala musanagunditse chipumi chanu pansi. Kuyang’ana mbali zonse za mphuno yanu muli pa Sajda. Kuyang'ana pa mapewa anu pamene mukuchita Salaam. Kwa munthu yemwe ali kumanzere kwa imam mu

Swalah ya Jama'at, achite niyyah kuti akulonjera angelo a Hafaza,[1] ndi Asilamu omwe achita nawo jama'at. Kwa munthu yemwe ali ku manja kwa imam, achite niyya kuti akulonjera angero a Hafaza ndi jama’at. Kwa munthu wopanda aliyense ku dzanja lake lamanja ndi lamanzere, achite niyya yake kuti akungolonjera angero a Hafaza. Osapukuta thukuta pa nkhope nthawi ya Swalah. Kupewa kutsokomola ndi kuyasamula. Maso ayang'ane pa ntchafu zanu pomwe mwakhala pa Tahiyyat. Kwa imam kutembenukira jama’at akamaliza Swalah.

ADAB[2] ZA SWALAH

1– Kwa munthu wochita Swalah payekha komanso kwa amene akuchita Swalah mu jama’at motsogozedwa ndi imam, anene pemphero ili akachita Salaam: “**Allahumma anta-s-salaam-u- wa minka-ssalaam tabarakta ya dhal-jalali wa-l-ikram.”** Kenako anene motere katatu: “**As taghfirullah-al’adhim al-ladhi la ilaha illa huw-al-hayyel-qayyuma wa atubu ilaih.”** Pemphero limeneli limatchedwa **Istighfar**. Ndi jaiz (zololedwa) kunena pemphero limeneli ngakhale munthu alibe udhu.

2- Kenako kunena ayah yotchedwa **Ayat-al-kursi.**

3- Kunena kuti, **“Subhanallah ,”** kokwana makumi atatu ndi mphambu zitatu.

4- Kunena kuti, **“Al-hamd-u-li-llah,”** kokwana makumi atatu ndi ndi mphambu zitatu .

5- Kunena kuti: **“Allahu akbar,”** kokwana makumi atatu ndi mphambu zitatu.

---

[1] Awa ndi angelo olemekezeka olembera. Awiri mwa iwo amapatdidwa kwa munthu aliyense; wina amalemba zabwino ndipo wina amalemba zoipa.

[2] Makhalidwe a chisilamu, kukhala ozindikira

6- Nenani pemphero ili kamodzi: “**La illaha ilallahu wahdahu la sharikalah lahul mulku wa lahul hamdu wa Huwa ’ala kulli shay’in qadir.”**

7- Kutambasula mikono yanu kutsogolo ndi kutsegula manja anu ku Arsh, komwe ndi ku Qibla, ndikunena pemphero lanu lopempha madalitso a Allah molungama ndi mochokera pansi pa mtima.

8- Ngati muli pa Swalah ya jama’at, mudikire pemphero lomwe muchitire limodzi.

9- Kunena, "Amin," kumapeto kwa pemphero.

10- Kupukuta ndi manja anu ku nkhope modekha (ku shukulu).

11- Kenako kunena Surah **Ikhlas** kokwanira ka khumi ndi kamodzi, pomayamba ndi Bismillah nthawi iliyonse mukusoma Surahyi. Uwu ndi mchitidwe wolamuridwa mu Hadth sharif yomwe yatchulidwa pa tsamba la gawo loyamba la bukhu lotchedwa **Beriqa.**

Kenako nenani ma ayah awiri omwe akuyamba ndi mawu oti, **"Qul-a'udhu...,"** kamodzi, ndipo kenako nenani, "astaghfirullah," kokwana makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zisanu ndi ziwiri (67). Kwaniritsani chiwerengero cha ‘astaghfirullah’ kufika pa makumi asanu ndi awiri (70) ponena pemphero lonse la Istighfar katatu. Tsopano nenani kuti, “**Subhanallahi wa bihamdihi subhanallah-il adhim**,” kokwanira khumi. Pambuyo pake ndi kudzanena ayah yonse yoti: **“Subhana Rabbika...”** Adabu zimenezi zalembedwa m’bukhu lotchedwa **Meraq-il-felah.** Zanenedwa motere mu Hadith-i-Sharif: **“Mdalitso woperekedwa mutamaliza kuswali swalah iliyonse mwa swalah zisanu za pa tsiku adzalandiridwa** ndi Allahu ta’âlâ.” Komabe mdalitso woperekedwa ndi mapemphero ena aliwonse otumizidwa ayenera kuchitika mowona mtima komanso mwakachetechete. Ndi makruh kuperaka mdalitso kapena kunena mapemphero ena pakutha pa swalah zisanu za patsiku zokha kapena pa nthawi zina zokhazikitsidwa kapena kulakatula ndakatulo yomwe inalowezedwa m’dzina la mdalitso kapena mapemphero.

Pamene mdalitso kapena mapemphero atha, ndi Sunnah kupukuta ku nkhope ndi manja anu modekha. Mtumiki Swalla Allaahu alaihi wa sallam amanenanso mapemphero ake atatha Tawaf (kuzungulira Kaaba), atamaliza kudya, komanso asanagone. Nthawi ya mapemphero otere, iye samatambasula manja ake odalitsika, ndipo sanali kusisita manja ake odalitsika pa nkhope yake yodalitsika. Mapemphero ochitika, mdalotso woperekedwa, ndi dhikr za mtundu wina uliwonse ziyenera kuchitika mwakachetechete. Ndi mustahab kukhala ndi udhu pamene mukupereka mdalitso kapena kunena

mapemphero ena monga Istighfar. Ndi haram kuvina, kuliza likweru, kuwomba m'manja, kuliza zida zoyimbira monga ting'oma, zitoliro, bango, ndi zingwe ziri zonse. Mchitidwe umenewu wachulukira mwa anthu abodza a Tasawwuf (Ma Sufi). Zoti izi ndi haram zanenedwa ndi akatswiri a Chisilamu onse pamodzi.

Monga zikuwonekera, ndi zolimbikitsidwa kwa Asilamu oswali pa jama'at mosogozedwa ndi imam kunena mapemphero awo kapena kupereka madalitso awo mwakachetechete. Komanso ndi zololedwa aliyense kunena pempho pa yekha ngakhale kungodzuka ndi kutuluka popanda kunena pempho lawo. Zanenedwa motere m'bukhu lomwe mutu ndi **Fatawa-i-Hindiyya**, lokonzedwa ndi gulu la akatswiri motsogozedwa ndi Shaikh Nizam Mu'in-ud-din Naqshibandi: "Mukatha kuswali Swalah yomwe ili ndi Sunnah kumapeto kwake, monga swalah ya masana (Dhuhr), ya madzulo (Maghrib), ndi ya usiku (Isha), ndi makruh kwa imam yemwe watsogolera mbali ya Swalah ya fardh pa jamaat kukhala pansi atachita salaam. Akangonena salaam ayenera kuswali Sunnah yomaliza atasuntha cha kumanja kapena cha kumanzere kapena cha kumbuyo pang'ono. Kapena, akhoza kutuluka kupita ku nyumba, ndi kukachita Sunnah yomaliza kunyumba. Asilamu omwe amachita jama'at, komanso Msilamu yemwe wachita Swalah pa yekha, akhoza kukhala pansi ndi kunena mapempho awo. Ndi zololedwanso kwa iwo kuyima ndi kuchita Sunnah yomaliza pamalo omwe anakhala kapena kusuntha pang'ono cha kumanja kapena cha kumanzere kapena cha kumbuyo.

Mu Swalah imene ilibe Sunnah yomaliza monga Fajr ndi Asr, ndi makruh kuti imam akhalebe molunjika Qibla; Ndi mchitidwe wa bid'at. Ayenera kudzuka ndi kuchoka kapena kutembenukira ku jama'at kapena kutembenukira kumanja kapena kumanzere kenako ndi kukhalanso pansi."

MAPEMPHERO (kapena Ma Dua woperekedwa) KUMAPETO KWA SWALAH

"Al-hamd-u-li-l-lahi Rabb-il-'alamin. As-salatu wa-s-salaamu 'ala Rasulina Muhammadin wa 'ala Alihi wa Sahbihi ajma'in. Ya Rabi (Oo Mbuye wanga, Allahu ta'âlâ)! Chonde vomerezani Swalah yomwe ndachita! Chonde ndidalitseni ndi khayr (ubwino) mu akhir (moyo wotsiriza) wanga ndi mu aqibat (mapeto anga). Ndidalitseni ndi mwayi wonena Kalima-i-Tawhid pakupuma kwanga komaliza, (pomwalira). Dalitsani abale anga akufa ndi 'afw ndi maghfirat (chikhululuko ndi

chifundo) chanu. Allahum-maghfir warham wa anta khayr-urrahimin. Tawaffani Musliman wa-al-hiqni bi-s-Saalihin. Allahummaghfirli wa-li-walidayya wa-li-ustaziyya wa-li-lmu'minina wa-l-mu'minat yawma yaqum-ul-hisab. Ya Rabbi! Nditetezeni ku zoyipa za Satana ndi zoyipa za adani ndi zoyipa za nafs-i-ammara (zilakolako zanga)! Chonde dalitsani nyumba yathu ndi zabwino ndi halal ndi riziki labwino (chakudya, ndi zina zotero).

Chonde dalitsani ahl-i-Islam (Asilamu) ndi salamat (chipulumutso, chitetezo chanu)! Chonde awonongeni a'dayi-muslimin, (adani a Asilamu!) Chonde thandizani Asilamu amene akuchita Jihad kwa osakhulupilira, ndipo adalitseni ndi thandizo Lanu! Allahumma innaka 'afuwwun karimun tuhibb-ul-'afwa fa'fu 'anni. Ya Rabbi! Dalitsani odwala athu ndi umoyo wabwino ndi ovutika omwe ali pakati pathu ndi mpumulo! Allahumma inni as'aluka sihhata wa-l-afiyata wa-l-amanata wa husn-al-khulqi wa-r-ridaa bi-l-qadari bi-rahmatika ya arham-ar-rahimin. Chonde dalitsani makolo anga ndi ana anga ndi abale anga ndi anzanga ndi abale anga onse Achisilamu ndi moyo wokongoletsedwa ndi khayr ndi husn-i-khulq ndi umoyo wabwino wa rushd-u-hidayat ndi istiqamah, ya Rabbi! Amin. Wa-l-hamd-u-li-l-lahi Rabb-il'alamin. Allahumma salli 'ala sayyidina Muhammadin wa'ala Ali-Muhammad kama sall-ay-ta 'ala Ibrahima wa 'ala Al-i-Ibrahim innaka Hamid-un-Majid. Allahumma barik 'ala Muhammadin wa 'ala Al-i-Muhammad kama barakta 'ala Ibrahima wa 'ala Al-Ibrahim innaka hamid-un-majid. Allahumma Rabbana atina fi-ddünya hasanatan wa qina 'adhab-an-nar birahmatika ya-Arhamar-rahimin. Wa-l-hamd-u-li-l-lahi Rabb-il-'alamin. Astaghfirullah, astaghfirullah, astaghfirullah, astaghfirullah-al-'adhim al-karim alladhi la ilaha illa Huw-al-Hayy-al-Qayuma wa atubu ilaih."

ZOMWE ZILI MAKRUH PA SWALAH

1-Kupinda khosi poyang'ana mbali zonse.

2- Kuseweretsa chinthu china chake uli pa swalah.

3- Popanda 'udhr, (chifukwa chomveka chochitira zimenezo) kusesa ndi dzanja pa malo ochitira sajda nthawi ya Swalah.

4- Kwa amuna, ndi makruh kuyika manja awo pa chifuwa atayima pa Swalah, komanso ndi makruh kuyika manja pa mu mzere umodzi ndi chifuwa pochita sajda.

5- Kuwongola dzala zanu pozithyola ndikuti zimveke kulira.

6- Kukhala chopingasa miyendo popanda 'udhr.

7- Kukweza mwendo wanu umodzi pa nthawi ya Sajda.

8- Pamene mukuchita Swalah, kuvala chinthu chomwe simungavale pamaso pa akuluakulu anu kapena adindo anu.

9- Kuchita Swalah moyang'anizana ndi nkhope ya munthu wina.

10- Kuchita Swalah moyang'anizana ndi moto.

11- Kukhala ndi chojambula kapena chithunzi pa thupi lanu kapena pa chovala kapena choswalila.

12- Kuyasamula popanda ‘udhr kutero.

13- Kuchita Swalah manja anu ali okhutiridwa mkati mwa chovala chanu.

14- Kukhala moyimika miyendo yanu ngati galu.

15- Kutseka maso anu (kutsinzina).

16- Kusayang'anitsa manja anu ku Qibla.

17- Pochita Swalah pa jama’at, kuyima pa mzere wakumbuyo pomwe pali malo okwanira munthu mmodzi pa mzere wa pa tsogolo pake. Ndi tanzihi karahat (makruh) ngati pali anthu ena ndi pa mzere wakumbuyowo, koma ndi tahrimi karahat ngati palibe wina woyima ndi inu. Zikatero ndiye kuti inu mwasiya wajib; Kulakwitsa uku kungakonzedwe pobwereza kuchita Swalahiyo.

18- Kuchita Swalah moyang'anizana ndi manda popanda chotchinga pakati panu ndi manda.

19- Kuchita Swalah moyang'anizana ndi najasi (zinthu zauve, zanyansi).

20- Kuti mamuna ndi mkazi achite Swalah zosiyana pomwe wina ali pa mbali pa mnzake.

21- Kuchita Swalah uku mukufunitsitsa kupita ku chimbudzi.

22- Mukayima kuchoka pa Ruku, popita pa Sajda kuyamba kugunditsa manja pansi mawondo asanagunde pansi, popanda ‘udhr yopangira choncho.

23- Kuzikanda mbali iriyonse ya thupi lanu kawiri mkati mwa rakat imodzi. Rakat imayamba pa nthawi yoyima koyamba kwa Swalah ndi kuthera pa kuyima kwachiwiri. Swalah yanu idzakhala fasid (yopanda pake) mukakweza dzanja lanu katatu ndi kuzikanda katatu. Swalah yanu iyenera kubwerezedwa.

24–Mukakhala pa Swalah ya jamaat, kuwerama pa ruku imam asanatero.

25- Kuweramuka mwa changu kuchokera pa ruku imam wanu asanatero.

26- Kuchita Sajda mwachangu imam asanatero.

27- Kunyamuka pa Sajda nsanga imam asanatero.

28- Kuyimilira pogwirira chinthu chomwe chili pafupi nanu, pokhapokha mutakhala ndi ‘udhr yochititsa kuti simunagachitire mwina.

29- Pochokera pa Sajda, kunyamula mawondo anu musananyamule manja anu kuchokera pansi kapena pa mswala.

30- Kusasa fumbi ku nkhope ndi m’maso.

31- Mu rakat ina iliyonse yotsatira, kulumpha Surah yotsatira Surah imene munawerenga pa raka’at yoyambilirayo.

32- Kuwerenga sura imodzi yomweyo m’marakat awiri otsatizana, kapena kuwerenga Surah imodzi yomweyo kawiri mu raka’at imodzi. Izi ndi zololedwa mu Swalah ya nafila [ibadat yongoonjezera]

33- Mu rak'at ina iliyonse yotsatira, kuwerenga Surah yomwe ili kutsogolo kwa Surah imene inawerengedwa mu rakat ya pambuyu.

34- Mu rakat ina iliyonse yotsatira, kuwerenga ma ayah atatu kupyola ma ayah omwe ali mu dhamm-i-Surah yomwe munawerenga mu rakat yapitayo.

35- Kuwerama kapena kuweramuka pogwilira chinthu chomwe chili pafupi, pokhapokha mutakhala ndi ‘udhr, (chifukwa chabwino chololedwa m’Chisilamu), chomwe chikukukakamizani kutero.

36- Kuyingitsa ntchentche.

37- Kuchita Swalah ndi chovala chopinda manja kapena chomwe mapewa anu kapena mapazi akuwonekera.

38- Kulekelera osavala moyenera koyenda.

39- Kuchita Swalah pa njira.

40- Pochita ruku kapena Sajda, kuwerenga tasbih ndi zala zanu.

41- Imam kukhala mkati mwa mihrab moti kuyika katani sangawoneke ku jama’at.

42- Imam kukhala pokwelerapo kapena potsika kusiyana ndi jama’at pa mlingo woposa dhra’ imodzi ngati atakhalapo yekha. (Dhra’ imodzi ndiyofanana ndi theka la mita.)

43– Kuti imam atsogolere Swalah ya jama’at pa malo ena posakhala mu mihrab.

44- Kuyankha Amin mokweza mkati mwa Swalah.

45- Kumaliza Surah Fatiha kapena dhamm-i-Surah mutachoka kale pa qiyam, ndipo muli kale pa ruku.

46- Zonenedwa pa ruku -“Subhana Rabb-iy-al ’adhim”, kudzazinena mutaweramuka ndi kuwongoka pa kuyimilira komwe kumatchedwa qiyam.

47- Kuyima ndi phazi limodzi popanda chifukwa chilichonse chomveka chotchedwa udhr.

48- Kugwederagwedera pa Swalah.

49- Kupha nsabwe ndi zina zotero zoti ndi zosaluma.

50- Kununkhiza chinthu pa Swalah.

51- Kuchita Swalah wopanda chovala pa mutu. Ochita Hajj amachita Swalah opanda kuvala kanthu pa mutu poti amakhala atavala Ihram.

52- Kuyamba kuchita Swalah manja osavala.

53- Kuyamba kuchita Swalah ndi mapazi osavala kalikonse. (Malinga ndi qawl ina, ndi makruh mkazi kuchita Swalah wopanda kuphimba phazi ake. Malinga ndi kunena kwa qawl Swalah ya mkazi yemwe sanaphimba maphazi ake imakhala yopanda phindu. Kwalembedwa pa tsamba 439 m’bukhu la Ibni Abidin ndi makruh kusiya nsapato ndi zina zotero penapake chakumbuyo kwanu.” Zalembedwa kumapeto kwa **Bariqa** kuti ndi Sunnah kuziyika penapake kumanzere kwako, mmalo mwa penapake kutsogolo kapena ku dzanja lako lamanja.

Zalembedwa mu **Targhib-us-salat** kuti ndi makruh kunena mapemphero monga pemphero lotchedwa 'evrad' pakati pa Swalah za fardh ndi Sunnah.

ZOWONONGA SWALAH

Mu Madhhab a Hanafi mwatchulidwa zinthu makumi asanu ndi zisanu (55) zomwe zingachititse Swalah yanu kukhala yopanda phindu. Izi sizitengera kuti zinthuzo zachitika modziwa kapena mosadziwa:

1– Kuyankhula pa Swalah

2– Kuseka mokweza moti wosekayo ndikudzimva yekha.

3- Kuchita chinthu chomwe tinganene kuti ndi amal-i-kathir.

4- Kulumpha sitepe imodzi mu Swalah popanda udhr.

5- Kusiya kuchita chinthu kapena sitepe imodzi ya mu Swala mongofuna kutero.

6- Kufuula mokweza pa chinthu cha pa dziko.

7- Kutsangula kukhosi kapena kutsokomola popanda udhr.

8- Kutafuna chingamu.

9- Kuzikanda pa chiwalo chirichonse katatu ndi dzanja limodzi, kapena kukweza manja anu ndikuwomba m'manja mu rakat imodzi.

10- Kugwirana chanza (ndi wina).

11- Osanena takbir ya iftitah mokweza moti ndi kuyimva nokha.

12- Kusanena Sura ndi mapemphero a mu Swalah molimbika koti nokha ndikumva.

13- Kunena kuti, “La hawla wala quwwata il-la billah-il-’aliy-yil ’adhim,” kapena “Subhanallah,” kapena “La illaha ilallah,” pamene wina wakuyitanani. Swalah yanu siyidzakhala fasid (yopanda pake) ngati cholinga chanu ndikuwadziwitsa kuti mukuchita Swalah. Komabe, idzawononga Swalah yanu ngati cholinga chanu ndi kuyankha munthuyo.

14- Kuvomera moni mwadala.

15- Kulawa chinthu chotsekemera mkamwa mwanu, ndi kuti madzi ake alowa kukhosi kwanu.

16- Pamene mukuchita Swalah panja, kutsegula pa kamwa mutayang’ana kumwamba, ndipo madzi a mvula, matalala, kapena zina zotere, kugwera ku m’mero kwanu.

17- Kukoka chingwe cholondolera nyama (yomwe mukukwera) katatu.

18- Kukweza dzanja lanu katatu kapena kupha nsabwe, utitiri kapena zina zotere pozikanikiza.

19- Kuzula tsitsi litatu mkati mwa rakat imodzi.

20- Kutchula liwu la mamvekedwe a patatu monga damn, puff, ndi ena.

21- Pomwe mukuchita Swalah pa hatchi m'njira yovomerezeka ndi Chisilamu, kuyigunda katatu ndi mwendo umodzi.

22- Kulimbikitsa kamodzi ndi mapazi onse awiri.

23- Pochita Swalah pa jama’at, kuyimilira imam asanayimilire.

24- Kuyenda ndi kusuntha pakati pa mizere iwiri popanda ‘udhr, yovomerezeka kutero m’Chisilamu.

25- Kupesa tsitsi lanu kapena ndevu.

26- Kuti mamuna ndi mkazi achite Swalah mbali ndi mbali pa mzere umodzi pa mbuyo pa imam - mu Swalah ya jama’at yomwe imam akutsogolera ndi cholinga chokhala imam (wa gulu la) amuna ndi akazi. (Ndi zololedwa ngati iwo sali mu mzere umodzi kapena mbali ndi mbali, kapena pakati pawo pali katani lotchinga. Ndi haraam kwa akazi

ndi atsikana kutuluka popanda kudziphimba kumutu kapena m'manja mwawo moyenerera, mwachitsanzo kusiya mbali za awrat zawo zikuonekera kaya akupita ku mzikiti, kapena kokayenda. Ntchito za kupembedza zomwe angachite ali chonchi zidzawabweretsera utchimo osati thawab, [malipiro a tsiku lomaliza.])

27- Kuthandiza imam yemwe asakutsogolera Swalah yomwe mukutsatira. Kutanthauza imam yemwe akutsogolera jammat ina ndipo akudodoma powerenga ma Ayah.

28. Tiyerekeze kuti mkazi wayima pamalo opanda munthu ndi kuyamba kutsata imam ndipo kenako amuna ena afika ndipo mizere yatsopano ya jama'at yayala moti malo a Swalah a mkazi aja atsekeka; Swalah ya amuna atatu idzakhala fasid: mamuna yemwe ali pafupi kudzanja lake lamanja la mkaziyo, yemwe ali pafupi kumanzere kwake, ndi yemwe ali pambuyo pake.

29- Kukumbatira mwana wanu.

30- Kudya kapena kumwa kanthu.

31- Kumeza chinthu chachikulu ngati nandolo chomwe chinatsalira pakati pa mano anu.

32- Kukumanitsa mbali ziwiri za kolala yanu ndi manja anu onse awiri, kapena kuvula chisoti chanu ndi dzanja limodzi kapena kuvula ndi kuchivalanso.

33- Kunena kuti, **"Inna lillah wa inna ilaihi raji'un,"** mutamva nkhani yosakhala bwino, yachisoni.

34- Kunena kuti, **"Al-hamd-u-lillah,"** mutamva nkhani yabwino.

35- Malinga ndi qawl, kuyetsemula ndi kunena kuti, **"Alhamd-u-lillah."**

36- Kunena kuti, **"Yarhamukallah,"** kwa munthu amene akuyetsemula pafupi nawe.

37- Kunena kuti, **"Yahdikumullah,"** pamene munthu wina akuyetsemula.

38- Kuti mamuna abwere kudzampsopsona mkazi akuchita Swalah.

39- Pochita Swalah, kupempha zinthu za padziko, monga golide ndi siliva.

40- Kutembenuza chifuwa chanu kuonetsa komwe kasali ku Qibla.

41- Kukweza mmwamba mapazi onse awiri pa nthawi ya Sajda.

42- Kuwerenga ma ayah a Qur'an mosokonekera kotero kuti tanthauzo lake lenileni ndi kusintha.

43- Kuti mkazi ayamwitse mwana wake.

44- Kusintha malo wina atakupempha kutero.

45- Kukwapula chiweto (chomwe mwakwera) katatu.

46- Kutsegula chitseko chotsekedwa.

47- Kulemba chinachake ndi zilembo zosachepera zitatu.

48- Kuvala mkanjo wanu.

49- Kukumbukira Swalah yanu ya Qada ngati ali ochepera asanu ndi imodzi.

50- Pochita Swalah ya fardh pomwe pali udhr- pa [chombo kapena sitima] kapena pamsana pa nyama (monga hatchi), kutembenukira ku mbali ina osati ku Qibla.

51- Kuyisenzetsa katundu nyamayo pamene muli pa msana pake.

52- Kukhala murtadd (wopanduka ku chipembedzo) ndi mtima wako.

53- Kukhala janab kapena kuti mkazi wayamba kuchita nsambo.

54- Kwa Imaam amene akutsogolera Swalah pa Jama'at, kulowetsa mzake mmalo ake chifukwa akuganiza kuti udhu wake wawonongeka.

55- Kusoma ma ayat a mu Qur'an mosintha mamvekedwe a zilembo zomwe zingaononge matanthauzo ake. [Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ" akunena motere pamene akuyamba nkhani yake pa Sunnah za Swalah: "Swalah yochitidwa potsatira munthu amene ali kunja kwa Swalah siyidzakhala sahih. Ndi makruh kwa imam kapena muazzin kukweza mawu awo molimbika kuposa mmene jama'at ingafunikire kuti iwamve.

Pomwe imam ndi muazzin akunena takbir ya iftitah pa nthawi imene akuyamba kuchita Swalah ya jama'at, iwo achite niyyah kuti akuyamba kuchita Swalah. Swalah yawo siyidzakhala Sahih ngati achita Niyyah (cholinga) yongoti mau awo amveke ku jama'at. Ndipo Swalah ya anthu otsatirawo siyidzakhala sahih. Ndi makruh kwa muazzin kubwereza ma takbir mkati mwa Swalah mokweza ngati liwu la imam likumveka mokwanira. Ndi bidah yowopsya kuchita izi Ndi mustahab kwa iwo kutero ngati kuli kofunika, koma ndiye kuti Swalah ya muazzin idzakhala fasid ngati akuchita izi ndi cholinga chongokometsera. Ndi chifukwa chake, ma imam ndi ma muazzin omwe akugwiritsa ntchito zimkuza mau ndi cholinga choti mawu awo amveke amachititsa jama'at' Swalah yawo kukhala fasid komanso amalepheretsa kuti Swalah yawo isakhale sahih. Ndi bidah yowopsya dzedi. Ndipo ndi tchimo lalikulu kuchita bidah. Sizili Sahih kuswali potsatira Imam amene akuchita Swalah mu Jama'at kudzera pa wailesi yakanema. Zalembedwa ndi umboni m'nkhani ya m'magazini

otchedwa **al-Mu'allim**, ya khumi ndi chiwiri (12) yomwe inatuluka mu Rabi'ul-awwal, 1406, (December 1985), yofalitsidwa ndi akatswiri a maphunziro a ku India ku Malappulam.]

Nanga ndi ziti zomwe siziwononga Swalah yanu: Kusuntha sitepe imodzi kapena ziwiri kupita pa tsogolo panu ngati pali mzere woti uli ndi malo; kunena "Amini," osati poyankha munthu; kuvomera malonje a munthu wina pochita chizindikiro ndi diso lanu kapena zikope, -wina akati, "Salaamun alaikum,"; wina akakufunsani kuti mwachita ma rak'at angati ndipo inu ndikusonyeza zala ziwiri ngati yankho. Zimenezi zizingawononge Swalah yanu.

Tanthauzo lenileni la 'salat' ndi 'chifundo ku mbali ya Allahu subhânahu wa ta'âlândi istighfar ku mbali ya angelo ndi mapemphero ku mbali ya okhulupilira'. Tanthauzo laukadaulo ndi 'af'al-i-ma'luma ndi arkan-i-mahsusa', yomwe ndi 'Swalah' mu Chichewa. Af'al-i-ma'luma ndi 'zochitika zomwe timachita kunja kwa Swalah, ndipo ar-kan-i-mahsusa ndi ma rakat, zomwe talamulidwa (kayimidwe pa Swalah, kakhalidwe pa Swalah, momwe tingazigwedezere, ndi mapemphero athu), ndipo zina zonse zoyenera pa Swalah.

Tsiku lina, Rasulullah sall-Allahu 'alaihi wa sallam, poyamikira mwa padera munthu wodalitsika kwambiri kwa iye, adauza Hadrat 'Ali karrim-Allahu wajhahu wa "radiyallâhu 'anh": **"Oooh Ali! Uyenera kuchita Swalah za fardh, wajib, Sunnah, ndi mustahab."**

Pamenepo Sahabi wodalitsika mwa ma Ansar[1] adati: Ya Rasulullahah (E, Mtumiki wodalitsika wa Allahu ta'âlâ)! Hadrat 'Ali akudziwa kale zinthu zonsezi. Tiuzeni za ubwino wochita Swalah za fardh, wajib, Sunnah ndi mustahab kuti tichite moyenera. Hadrat Rasulullah sall-Allâhu 'alaihi wa sallam anati: "**E, inu Ummat wanga ndi ma Sahabah anga! Swalah ndi chomwe Allahu subhânahu wa ta'âlâamakondwera nacho. Ndi zimene Angelo amakonda. Ndi Sunnah ya Atumiki. Ndi nur** (dangalira) **ya ma'rifat** (chidziwitso cha chinsinsi cha Allah)**. Ndi amal** (ntchito) **zabwino kwambiri kwa mchisilamu**. **Ndi mphamvu ku thupi**. **Ndi baraka ya rizik. Ndi nur ya uzimu. Ndi kulandiridwa kwa mapemphero. Ndi muwomboli kwa**

[1] Pamene Wabwino wa Anthu, Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" adasamuka kupita ku Madina (kuchokera ku Makka) m'chaka cha 622 A.D., Asilamu omwe ankakhala ku Madina anakumana naye mosangalala kwambiri ndipo anamusunga Mtumiki wodalitsi-kayu ndi maSahaba ena omwe anasamuka pambuyo ndi ulemelero. Osamukawo amatchedwa 'Muhajir' (ambiri. Muhajirin) ndipo Asilamu aku Madina omwe anathan-diza iwo atchulidwa'Ansar'.

Mngelo wa imfa. Ndi nyali ya m'manda. Ndi yankho kwa Hadrat Munkar ndi Nakir (angelo ofunsa otchedwa)**. Lidzakhala denga pa lanu pa tsiku lachiweruzo**. **Ndi katani pakati pa Jahannama ndi inu**. **Idzakuwolotsani pa Sirat ngati mphezi. Ndi chisoti chachifumu pamutu wanu ku m'Paradiso. Ndi makiyi aku mParadiso."**

PHINDU LA SWALAH YA JAMA'AT

Tiyerekeze kuti munthu waswali ma rak'at awiri mu jama'at ndi kuswali ma rak'at makumi awiri ndi asanu ndi awiri (27) payekha, Swalah ya ma rak'at awiri a mu jama'at idzamupatsa thawab zambiri kuposa Swalah ya rak'at 27 zomwe waswali pa yekha.

Malinga ndi riwayat ina (mafotokozedwe a akadaulo a Chiphunzitso), ngakhale Swalah yochita pa yekha itakhala ndi rakat chikwi, rakat ziŵiri za Swalah ya mu jama'at zidzamupatsabe thawab zambiri. Pali thawab zambiri pakuchita Swalah pa jama'at. Nawu wina mwa ubwino wake:

1– Okhulupilira akasonkhana pamodzi, adzakondana.

2- Osadziwa adzaphunzira zochita zokhudza Swalah kuchokera kwa ophunzira.

3- Ngati Swalah ya ena mwa iwo ili yovomerezeka pomwe ena siili yovomerezeka, Swalah ya gulu losavomerezekalo idzalandiridwa pa chisomo cha Swalah yovomerezekayo.

Hadith sharif ikunena kuti: **"E, inu Ummat wanga ndi ma Sahabah anga! Ndakusiyirani njira ziwiri: Imodzi mwa izo ndi Qur'an al-'adhim ush-shân, ndipo ina ndi Sunnah yanga. Munthu amene atsate njira ina osati ziwiri izi si Ummat wanga!"** ['Abd-ul-Ghani Nablusi "rahima-hullâhu ta'âlâ" (1050 [1640 AD], Damascus - 1143 [1731]) akunena motere mu tsamba la makumi asanu ndi anayi ndi mphambu zisanu ndi zinayi (99) la bukhu lake lotchedwa **Hadiqa** (yomwe ndi ndemanga yake ku bukhu lotchedwa **Tariqat-i-Muhammadiyya** lolembedwa ndi Imam Birgivi: Pomwe Allahu subhânahu wa ta'âlâ analengeza gawo lina la chiphunzitso cha Chisilamu kudzera m' Qur'an al-kareem, analengeza gawo lina kudzera mu Sunnah za Mtumiki Wake wodalitsika "sallallâhu alaihi wa sallam". Sunnah za Rasulullah muli zikhulupiliro zake, zoyankhula zake, zochita zake, chikhalidwe chake, ndi ukadaulo wake povomereza ntchito za ena kapena zoyankhula zao, [zomwe zimayimura kuvomereza kwake pa zochitika kapena kunenedwa)]" Hadithi sharif iyi ikuwonetsa gawo la chiwiri la (Magwero anayi a chidziwitso mchisilamu) **Edilla-i-shar'iyya**.]

KUTSOGOLERA MU SWALAH YA JAMAAT (IMAMAT)

Pali mitundu inayi ya anthu omwe amatsatira imam mu Swalah ya jama’at: Mudrik, Muqtadi, Masbuq, ndi Lahiq.

1- Mudrik ndi Msilamu amene amachita takbir iftitah pamodzi ndi imam. Imam akati: “Allahu akbar,” naye amachita pafupifupi munthawi yomweyo. Zomwe zikutanthauza kuti wayamba kuchita Swalah mu jama’at motsogoleredwa ndi imam.

2- Msilamu amene waphonyana ndi takbir iftitah amatchedwa muqtadi.

3- Masbuq ndi Msilamu yemwe amayipeza jama’at ndi kuyamba kutsatira imam koma imam atachita kale rakat imodzi kapena ma rakat awiri a Swalah.

4- Lahiq ndi Msilamu amene anachita takbir iftitah pamodzi ndi imam; ndikupezeka kuti hadas yamupeza, (mwachitsanzo udhu wake waduka;) ndiye wakachita udhu ndi kuyambanso Swalah pambuyo pa imam. Msilamu ameneyu amachita Swalah monga momwe amachitira pamene adali kumbuyo kwa imam (sachita qiraat, koma amachita Ruku, Sajda ndi tasbih pa nthawi yake). Ngati sanayankhule zili zonse za pa dziko (pamene amatuluka mu Msikiti kuti akakonzenso udhu wake), adzakhala ngati anachita Swalah yonse pambuyo pa imam komanso pamodzi ndi imam.

Koma akatuluka mu mzikiti kukachitenso udhu, ayenera kuchita udhu pa malo omwe ali pafupi ndi mzikitiwo. Pali akatswiri a Chisilamu amene amanena kuti Swalah yake idzakhala fasid akapita kutali kwambiri.

Munthu akulowa mu mzikiti ndi kumpeza Imam akuchita ruku, iye ndi kofulumira kuti amupeze Imam pochita takbir iftitah uku akuwerama pa ruku; iye sanatsatire Imam ndipo sanalowe mu Jama'at. Koma ngati akampeza imam akuchita ruku, iye ndikuchita niyyah yake kuti atsatire Imam, ndikuchita takbir (iftitah) yokhazikika pamalo oyima ndi kuwerama kupita pa ruku ndi kunena tasbih imam akanali pa ruku, iye wagwirana ndi imam ndipo walowa mu jama'at mkati mwa rakat imeneyo. Koma ngati imam akuweramuka pamene Msilamuyu akuwerama kupita pa ruku, ndiye kuti iyeyo sanayipeze rakat imeneyo.

KUKHAZIKIKA PA SWALAH (TA'DIL-I-ARKAN)[1]

Ngati munthu salabadira za ta'dil-al-arkan ndipo akudumpha m'malo asanu a Swalah mwadala, Swalah yake imakhala fasid (yopanda pake); izi zili chonchi malinga ndi Imam Abu Yusuf "rahima-hullâhu ta'âlâ". Malinga ndi Tarafeyn (Imam A'zam Abu Hanifa ndi Imam Muhammad), sizikhala fasid, koma kuti Swalah imeneyo idzayenera kubwerezedwa ndi cholinga chofuna kukonza kuonongeka kwake komwe kunachitika chifukwa cha kunyalanyaza kwa chinthu chomwe chili wajib. **Sajda-i-sahw** idzakhala yofunika mukalephera kuyisunga ta'dil-i-arkan moyiwala. [Chonde onaninso gawo la bukhu lino lomwe likunena za zomwe zimayambitsa kutaya iman!]

Kusalabadira ta'dil-i-arkan kumayambitsa zovuta makumi awiri ndi zisanu ndi chimodzi:

1– Kumayambitsa umphawi.

2- Ulama (akadaulo) a patsiku lomaliza amakudani.

3- Mumachoka mgulu la 'adalat (anthu a chilungamo), koti simungaloledwenso kukhala mboni.

4- Malo amene mwachitirapo Swalah (yosakwanira) adzakuyikirani umboni oyipa patsiku la lowuka.

5- Munthu adzakhala wotchimwa chifukwa cholephera kuchenjeza mwa chifundo komanso mwa nzeru munthu wina amene akumuwona kuti akuchita Swalah mosalabadira ta'dil-i-arkan.

6- Ndi wajib kubwereza Swalah yomwe mwachita mosalabadira ta'dil-i-arkan.

7- Zimachititsa kufa ulibe iman.

8- Umakhala mbava yobera Swalah.

9- Swalah imene mwayichita idzatayidwa ngati chisanza cha kale m'mano mwanu patsiku la Chiweruzo.

10- Mudzamanidwa chifundo cha Allahu ta'âlâ.

11- Mudzakhala kuti mwasonyeza khalidwe loyipa m'mapemphero anu kwa Allahu ta'âlâ.

12- Mudzamanidwa thawab zochuluka zopezeka mu Swalah.

[1] Ta'dil-al-arkan m'mapemphero zimathanthauza kuchita rukn (mfundo) iliyonse ya pemphero monga qiyam, ruku, sajdah, ndi zina zotere modekha, mwaulemu komanso moyenera osachita changu.

13- Zimachititsa kuti thawab zomwe mukanapatsidwa m'mapemphero anu ena zitsekerezedwe.

14- Zimachititsa kuti Jahannama ikhale yokuyenerani.

15- Zimachititsa anthu osadziwa omwe akukuwonani kutsatira machitidwe anu oyipa ndi kunyozera ta'dil-i-arkan. Pachifukwa ichi, kuchimwa kwa munthu wa chipembedzo kudzadzetsa chilango chachikulu.

16- Mudzakhala munthu wotsutsa Imam wanu.

17- Mudzakhala mutasiya Sunnah pa nthawi ya yogonjera.

18- Mudzaputa Mkwiyo wa Allahu ta'âlâ.

19- Mudzakhala mukukondweretsa Satana.

20- Mudzakhala kutali ndi Mparadiso.

21- Mudzakhala pafupi ndi Jahannama.

22- Mudzakhala mutawuchitira nkhanza mzimu wanu.

23- Mudzakhala mutawudetsa nokha mzimu (Nafs) wanu.

24- Mudzalakwira angelo awiri -wa ku dzanja lanu lamanja ndi lamanzere.

25- Mudzakhala mutamudandaulitsa Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam".

26-Mudzayambitsa mavuto ku chilengedwa chonse. Pakuti, chifukwa cha tchimo lanu, mvulaidzasiya kugwa ndipo sikudzakhala chakudya, kapena padzakhala mvula yosatha, yomwe idzawononge mbewu, m'malo mozimeretsa.

SWALAH PA MAULENDO ATALI

Zalembedwa motere m'bukhu la **Ni'mat-i-islam** lolembedwa ndi Hadji Muhammad Zihni "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", 1262–1332 [1914 AD], Kupluce-Beğlerbeği, Istanbul: Ndi kololedwa nthawi zonse, paliponse, kuchita Swalah ya nafila (ibada yongoonjezera) chikhalire ngakhale ndi kotheka kuchita mutayima. Pamene muchita Swalah chokhala, weramakani thupi lanu pa ruku. Pa Sajda ikani mutu wanu pansi pa chopemphelera. Komabe kuchita Swalah chokhala popanda udhr (chifukwa chabwino chovomerezeka ndi Chisilamu) kumapangitsa kuti okhulupirira alandire theka la thawab zomwe akanapeza atachita Swalah atayima. Swalah za Sunnah za ma Swalah a Fardh a sanu apa tsiku ndi Swalah za Tarawih ndi zina mwa Swalah za nafila. Mukakhala pa ulendo kupita kunja kwa matawunikapena madera a kumidzi, ndi kololedwa kuchita Swalah za nafila pa msana pa

nyama, (monga kavalo.) Sichokakamizika kutembenukira ku Qibla kapena kuchita ruku kapena Sajda. Mumapemphera pogwiritsa ntchito ima, (zizindikiro). Mwachitsanzo, mumawerama pang'ono thupi lanu pa ruku ndipo pa Sajda, mumawerama pang'ono mopitilira momwe munachitira pa ruku. Kuchuluka kwa Najasi pa nyama sikungawononge Swalah yanu. Ndi zololedwa kwa munthu amene watopa kuti pamene akuchita Swalah pansi atsamire ndodo kapena munthu wina kapena khoma. Si sahih (sizololedwa) kuchita Swalah mukuyenda. (Swalah yochita mukuyenda siyidzakhala yovomerezeka.) Pokhapokha pali udhr, Swalah za fardh kapena wajib, zisapempheredwe muli pa nsana wa chinyama chifukwa ngakhale muli kunja kwa mizinda. Udhr ikhoza kukhala chimodzi mwa izi: Kuwopa kuti anzanu apaulendo angakusiyeni nokha mukatsika pa chiweto chanu; kuwopa kuti pangakhale achifwamba mderalo oti angakupheni kapena kukulandani chuma chanu kapena chiweto chanu; pansi pali matope; mukatsika simuzathanso kukwera nyama yanu ndi zina zotero. Ngati ndi kotheka, imikani chiweto chanu poyang'ana ku Qibla ndikuchita Swalah yanu. Ngati sizingatheke, chitani Swalah yanu poyang'ana komwe chiweto chanu chayang'ana poyenda. Lamulo ili limagwiranso ntchito pochita izi pa bokosi la zinyalala lomwe limayikidwa pansana pa nyama. Ngati nyama yayimitsidwa, ndipo mlongoti wayikidwa pansi pa zinyalala, imasanduka kukhala **serir**, kapena kuti tebulo kapena sofa, kotero kuti kuchita Swalah pamwamba pake kuli ngati kuchitira pansi. Zikatero mudzayenera kuchita Swalah yanu mutayima uku mukuyang'ana ku Qibla.

Kuchita Swalah mu chombo kuyenera kuchitika monga momwe Rasulullah anaphunzitsira Hadrat Ja'fer Tayyar[1] pomwe Hadrat Ja'fer Tayyar amapita ku Abyssinia (Ethiopia) ndipo kuli motere:

Swalah ya fardh kapena wajib itha kuchitika mu chombo, ndipo sipafunika kukhala udhr pochita izi. Swalah ya jama'at itha kuchitika

[1] Ja'fer Tayyar "radiyallâhu anh" anali mmodzi mwa ana anayi a amalume ake a Rasulullah ochokera kwa Abu Talib. Iye anali wamkulu ndi zaka khumi kuposa Hadrat 'Ali ndipo wocheperako ndi zaka khumi kwa Hadrat 'Uqayl. Anasamukira ku Abyssinia ndipo anabwelera tsiku la Hayber. M'chaka chachisanu ndi chitatu [8] cha Hijrat (Hegira), anali pa nkhondo yolimbana ndi a Byzantine omwe anali ndi asilikali zikwi zitatu amphamvu pa malo otchedwa Mu'ta pafupi ndi Damasiko, pamene anaphedwa m'njira ya Allahu subhânahu wa ta'âlâ adani atamuunjilira ndipo analandira mabala oposa makumi asanu ndi awiri (70) tsiku limodzi. Anali ndi zaka makumi anayi ndi chimodzi. Iye adali m'modzi mwa anthu asanu ndi awiri omwe anali ofanana kwambiri ndi Rasulullah.

mu chombo. Ndi kosaloledwa kuchita Swalah pogwiritsa ntchito zizindikiro muli mu chombo. Ruku ndi Sajda ziyenera kuchitika. Komanso ndi kokakamizidwa kuchita molunjika ku Qibla. Mukamayamba kuchita Swalah, yimanii poyan'gana ku Qibla. Pamene chombo chikusintha kolowera, muyenera kutembenukira ku Qibla. Taharat (kudziyeretsa kuchokera ku Najasi) ndi kokakamizidwa mukakwera mu chombo. M'Madhhab a Hanafi, ndizololedwa kuchita Swalah ya fardh utakhala pansi mu chombo choyenda popanda kukhala ndi 'udhr.

Chombo chomwe chakhocheza pa gombe chili ngati chombo chomwe chikuyendabe pamadzi ngati kuli mafunde omwe akugwedeza mwamphamvu chombo chokhochezedwacho. Ngati chikugwedezeka pang'ono, chimakhala ngati ngalawa yomwe ili pafupi ndi gombe. Choncho sikotheka kuchita Swalah ya fardh mutakhala mu chombo chomwe chiri pafupi ndi gombe. Sizilinso sahih kuchita Swalah utayimirira, ngati kuli kotheka kupita ku mtunda.

Ndikofunikira kupita ku mtunda ndikukachita Swalah pa mtunda. Powopa kusowa kwa katundu kapena moyo wanu kapena kuti chombo chingakusiyeni, zimakhala zololedwa kuchita Swalah yanu m'chombo koma mutayima. Apa tikumaliza mawu athu kuchokera kwa **Ni'mat-i-islam.**

Zanenedwa mu Ibni 'Abidin kuti: "Kuchita Swalah pangolo yokokedwa ndi akavalo ya matayala awiri yomwe siyingathe kuyima pansi popanda kumangilira nyamayo ikuyenda kapena yangoyima, kuli ngati kuchita Swalah pansana pa nyama. Ngolo ya matayala anayi, ikayima ili ngati serir (tebulo, bed). Ikamayenda, Swalah ya fardh imatha kuchitika monga momwe zimakhalira udhr pa Swalah yochitira pa nyama; mumaiyimitsa, ndikuchita Swalah yanu poyang'ana ku Qibla. Mukalephera kuyimitsa, ndiye kuti muchita ngati mwakwera chombo pa madzi."

Munthu amene ali pa ulendo wautali wotchedwa 'safari' sangakhale pansi kapena kutembenukira ku Qibla mu chomwe wakwera, amatsanzira imodzi mwa Madhhab a Shafi'i kapena Maliki ndikuchita jam (kuphatikiza Swalah) za mapemphero awiri otsatizana akatsika chomwe wakwera.

Sizololedwa kwa munthu amene atha kukhala pansi kuti akhale pampando ndi kuchita Swalah ndi ima. Kuchita Swalah m'basi kapena m'ndege kuli ngati kuchita m'ngolo. Munthu amene wanyamuka ulendo wautali ndikuchita niyyah (cholinga) chake kuyenda mtunda wa masiku atatu, mwachitsanzo ma farsah = 54 mailosi [54 x 0.48 x 4

= 104 kilomita] kuchokera kunja kwa mzinda kapena mudzi, amakhala safari pamene akuchoka kunja kwa mzinda. Malinga ndi kunena kwa Ibni Abidin, mailo ndi ofanana ndi 4000 dhra', ndipo dhra' ndi yofanana ndi m'lifupi mwa zala makumi awiri ndi zinayi [24]. [Utali wa chala ndi wofanana ndi ma centimita awiri. M'Madhhab a Shafi'i ndi Maliki, ma farsah16 ndi chimodzimodzi 48 mailosi = 48 x 0.42 x 4000 = 80 km.]

Tabwerani, tiyeni tiswali, ndikuchotsa dzimbiri mmitima mwathu,

Simungayandikira kwa Allah ngati musakuSwali!

Mukangoswali, machimo anu amafutidwa,

Simungakhale oyera mpaka mutaswali!

Mu Qur'an al-kareem chilingamo chimatamanda Swalah kwambiri,

Imati: "Sindidzakukondani konse mpaka mutaswali!"

Hadith-i-sharif: "Iman sidzaonekera

Pa umunthu wanu ndipong'ono pomwe mpaka mutaswali!

Kusachita Swalah, ndi machimo akulu, mwa machimo onse,

Kulapa sikungathandize mpaka mutabweza Swalah zomwe munaphonya

osachita!

Wonyozera Swalah adzataya Iman yake poyera,

Sangapezenso Chisilamu chake mpaka ataswali!

Swalah imayeretsa mtima, ndi kuuchinjiriza ku zolakwa,

Siungathe kukhala owunikiridwa mpaka utaswali!

PHINDU LA TAKBIR YA IFTITAH[1]

Munthu akachita takbir iftitah limodzi ndi imam, machimo ake amagwa ngati masamba a mtengo m'chilimwe.

M'mawa winw Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" amachita Swalah pomwe munthu wina anafika mochedwa kwambiri moti sanachite nawo takbir iftitah ya swala ya m'mawayo ndi imam. Iye anachedwa ndi kumasula (kupereka ufulu kwa) kapolo. Pambuyo pake, anafunsa Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" kuti: "Ya Rasulullah (Eee, Mtumiki wa Allahu ta'âlâ!) Lero sindinathe kuchita

[1] Takbir iftitah ndi takbir yoyimitsila swalah.

nawo takbir iftitah ya swala ya m'mawa. Ndimamasula ndikupereka ufulu kwa kapolo. Sindikudziwa ngati ndidzapeza nawo thawab za takbir iftitah? Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anafunsa Hadra Abu Bakr "radiyallâhu ta'âlâ 'anh" kuti: **"Kodi munganene zotani za takbir iftitah imeneyi?"** Abu Bakr Siddiq "radiyallâhu anh" anayankha: "Ya Rasulallah subhânahu wa ta'âlâ "sallallâhu alaihi wa sallam"! Ndikadakhala ndi ngamira makumi anayi zoti zasenza zitsulo za mtenga wapatali monga mphete, makoza, ma nikelesi ndi zina zotero, ndikuzipereka zonsezo kwa osauka, sindikanapeza thawab zofanana ndi kuchita takbir iftitah ndi imam. Kenako anafunsa Hadrat 'Umar: **"Ee Umar! Kodi munganene chiyani za takbir iftitah iyi?"** Hadrat 'Umar "radiyallâhu anh" anati: "Ya Rasulullah subhânahu wa ta'âlâ "sallallâhu alaihi wa sallam"! Ndikadakhala ndi ngamira zambiri zoti kuzindanda ndikukwana mtunda wa pakati pa Makka ndi Madina, ndipo ngamila zonsezo ndikusenza zokometsera, ine ndikupereka zonsezo kwa osauka m'dzina la sadaka, sindingapeze thawab zofanana ndi thawab zopeza pochita takbir iftitah ndi imam." Kenako Mtumiki wodalitsika anafunsa kuti: **"Ee iwe Uthman, unganene chiyani za takbir iftitah iyi?** Hadrat 'Uthman zin-nureyn "radiyallâhu anh" adati: "Ya Rasulullah subhânahu wa ta'âlâ "sallallâhu alaihi wa sallam"! Ndikanachita Swalah ya ma rak'at awiri usiku ndikuwerenga Qur'an al-azeem ul shan yonse pa rakaat iliyonse, ndikadalephera kupeza thawab zomwe ndingapeze pochita takbir iftitah ndi imam." Pomaliza Hadrat 'Ali 'karrim-Allahu wejheh' anafunsidwa: **"Ee Ali! ukuti chiyani za takbir iftitah iyi?"** Iye anayankha motere: "Ya Rasulullah subhânahu wa ta'âlâ "sallallâhu alaihi wa sallam"! Kutakhala kuti osakhulupilira onse pakati pa kuzambwe ndi kummawa aukira kuti awononge Asilamu, ndipo Allahu ta'âlâ ndikundipatsa ine mphamvu ndikuchita Jihad ndi kupha osakhulupilira onse, sindingapeza thawab zofanana ndi zomwe zimaperekedwa pochita takbir iftitah limodzi ndi imam.

Ndipo Rasulullah subhânahu wa ta'âlâ "sallallâhu alaihi wa sallam"! Anati: **"Ee, inu Ummat wanga ndi ma Sahabah! Zikanakhala kuti zigawo zisanu ndi ziwiri za nthaka ndi zigawo zisanu ndi ziwiri za mitambo nkukhala pepala, nyanja zonse ndi kukhala inki, mitengo yonse ndi kukhala cholembera, ndipo angelo onse ndi kukhala mlembi, ndikumalemba (mosalekeza) kufikira tsiku la chimaliziro, akanalephera kulemba thawab zochita takbir iftitah ndi imam."**

Mwina mungafunse: "Kodi angelo olengedwa ndi Allahu adhîm-ush-shân ndi ochuluka kwambiri?" (Yankho ndi ili): Mu usiku wa Mi'raj, pamene Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anakwera kumwamba,

angelo amayendera Mparadiso, Jahannam ndi Bayt-i-ma'mur (Ka'ba) kenako ndi kumapita. Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" anafunsa kuti: **"Iwe m'bale wanga Jebrail! Angelo omwe akuzungulira Bayt-i-ma'mur sakubwereranso. Akupita kuti?"**

Jebrail "alaihim-salâm" anati: "Ya Habib Allahu (Okondedwa wa Allahu ta'âlâ)! Chiyambireni tsiku lomwe ndinalengedwa, sindinaonepo mngelo aliyense akubwereza kuzungulira Bayt-i-ma'mur. Mngelo akachita tawaf (kuzungulira Bayt-i-ma'mur, mwa kupembedza) ndikuchoka, nthawi yake siyidzabweranso mpaka Tsiku la Chiweruzo.

Munthu akanena Audhu… ndi Bismillah.. pa Swalah, Allahu subhânahu wa ta'âlâ amampatsa kapolo Wakeyo thawab zochuluka monga chiwerengero cha tsitsi la pa thupi pake. Kapolo akawerenga Fatiha-i-sharifa, Hadrat Allahu ta'âlâ amamupatsa thawab zofanana ndi zomwe akangapereke pa Hajj imene yavomerezeka. Kapolo ameneyu akawerama pa ruku, Allahu azeem ul shan amampatsa thawab zofanana ndi zomwe amapereka kwa amene apereka Golide zikwi ngati sadaka; ndipo akamachita Tasbih, (pomwe akunena kuti: "Subhana Rabbiy-al'adhim,") katatu, monga momwe akuphunzitsira mu Sunnah, Allahu adhîm-ush-shân amampatsa kapolo ameneyo thawab zochuluka ngati kuti wawerenga mabukhu anayi ovumbulutsidwa kuchokera kumwamba; komanso ngati kuti wawerenga ma suhuf zana (mabuku ang'ono akumwamba). Pamene akunena kuti, **"Sami' allahu liman hamidah,"** (pomwe akuwongoka kuchokera pa ruku), Allahu adhîm-ush-shân amamfungatira kapoloyo ndi nyanja za Rahmat (Chifundo, Chisoni). Akagwada kuchita Sajda Allahu ta'âlâ amampatsa kapoloyo thawab zambiri monga kuchuluka kwa chiwerengero cha anthu kuphatikiza ndi majini. Akanena Tasbih (Subhana Rabbiy-al-a'la) katatu, monga mwa lamulo la Sunnah, pali maphindu ambiri omwe Allahu azeem ul shan amapereka kwa kapolo Wakeyo. Ena mwa maphindu omwe atchulidwa ndi akatswiri a Chisilamu ali motere:

Phindu loyamba ndi kulandira thawab zolemera ngati kulemera kwa Arsh ndi Kursi. Chachiwiri, Allahu subhânahu wa ta'âlâ adzamupatsa kapoloyo maghfirat (Chikhululuko). Phindu lachitatu ndi loti kapoloyo akamwalira, Mikail „alaihim-salâm" (Mngelo wa chifundo) azidzamuyendera manda ake (kawirikawiri) mpaka tsiku lachimalizo. Cha chinayi, pa tsiku la Kiyama, Mikail „alaihim-salâm" adzamutenga kapolo ameneyo pa phiko lake lodalitsika,

adzamupempera iye chifundo ndi kupita naye ku Jannat-i-a'la (Mparadiso)[1].

Munthu akadzuka pa Sajda ndi kukhala pansi pa Qa'da-i- akhira (kukhala komaliza), Allahu azeem ul shan amamupatsa munthu ameneyo thawab zofanana ndi zomwe amapereka kwa ma fuqaray-i-sabirin (Asilamu osauka koma ali opilira).

Fuqaray-i-sabirin adzalowa ku Paradiso zaka ma zana asanu (500) kusanabwere ma aghniyay-i-shakirin (Asilamu olemera koma ali othokoza). Pamene aghniyay-i-shakirin adzawaona oyambawo, adzanena: "Tikanakonda tikanakhala ngati ma fuqaray-i-sabirin pa dziko lapansi!

M'manda angelo amafunso adzakufikira iwe;
"Umaswali mwadongosolo?" adzafunsa.

"Kodi mukuganiza kuti imfa yadzakupulumutsani?
Chilango chowawa chikukudikirani," adzanena.

MINDA YA PAMWAMBA YA KU MPARADISO(JANNAT-I-ALIYYAT)

Pali zipata zisanu ndi zitatu ndi makiyi asanu ndi atatu a Minda isanu ndi itatu yaku Mparadiso. Yoyamba ndi iman (chikhulupiliro) chomwe Okhulupilira amakhala nacho ndi kumaswali kasanu pa tsiku. Lachiwiri ndi Bismilla-i-sharifa, (kunena kuti, "Bismillah-ir-Rahman-ir-Rahim.") Zotsatira, zisanu ndi chimodzi zili mkati mwa Surah yoyamba ya Qur'an al-kareem yotchedwa Fatiha-i- shearifa. Ma Jannat asanu ndi atatu (Minda ya Mparadiso) ndi:

1– Dar-i-jelal. 2- Dar-i-qarar. 3- Dar-i-salaam. 4- Jannat-ul-khuld. 5- Jannat-ul-Me'wa. 6- Jannat-ul'adn. 7- Jannat-ul-firdevs. 8- Jannat-ul-na'im.

1- Dar-i-jelal ndi kwa nur yoyera.

2- Dar-i-qarar ndi kwa miyala ya rubi yofiira.

3– Dar-i-salaam ndi kwa miyala yobiriwira ya kirisoliti.

4- Jannat-ul-khuld kwa miyala ya makorali.

5- Jannat-ul-Me'wa ndi kwa siliva.

[1] Nkhani zabwino zonse zomwe zaperekedwa mpaka pano zikuphatikiza Asilamu onse, mosaona kuti ndi wamamuna kapena wamkazi.

6- Jannat-ul-’adn (Edene) ndi kokongoletsedwa ndi golide.

7- Jannat-ul-firdaws ndi kokongoletsedwa ndi golide ndi siliva.

8- Jannat-ul-na’im ndi kwa rubi yofiira.

Okhulupilira omwe adzalowe ku Mparadiso adzakhala m'menemo muyaya; iwo sadzatulukanso. Kumeneko kulibe nthawi ya msambo kwa azimayi kapena nthawi yodikira pambuyo pobereka; ndipo kulibe kulira kapena kudandaula. Chakudya kapena chakumwa chirichonse chimene adzafune chidzawapeza chili chokonza kale. Adzakhala kutali ndi mavuto monga kuphika ndi kunyamula. Mbalame zidzauluka pa mwamba pa mitu yawo. Okhulupilira azidzaziwona atakhala m'nyumba zawo zikuluzikulu zokongola.

"Tikanakhala kuti tili pa dziko lapansi ndipo iwe (mbalame) ndi kumandiyandikira kwambiri chonchi, ndikanakuwotchera." Chilakolakochi chotere kungofika mmitima mwawo, nthawi yomweyo mbale ya mbalame yongowotcha kumene yopangidwa ndi nur idzafika patsogolo pawo. Akamaliza kudya mbalameyo, okhulupilirayo azidzaunjika mafupa a mbalameyo malo amodzi ndi kulakalaka mu mtima mwawo kuti mafupawo akhalenso mbalame. Kulakalakako kungofika mu mtima mwawo, mafupa azidzabwerera kukhala mbalame ngati kale, ndipo mbalame yatsopanoyo izidzawuluka.

Dothi la ku Mparadiso ndi lopangidwa ndi mafuta onunkhira (musk) ndipo nyumba zake ndi za mdindo, zoti ina yopangidwa ndi siliva inzakeyo yopangidwa ndi golide.

Mamuna aliyense ku Mparadiso adzapatsidwa mphamvu za amuna zana limodzi (100). Aliyense mwa iwo adzapatsidwa akazi aku Mparadiso makumi asanu ndi awiri (70) ndi akazi awiri omwe anali padziko lapansi.

Kudzakhala mitsinje inayi ku Mparadiso. Yochokera gwero limodzi koma yosiyana mmayendedwe komanso kakomedwe. Umodzi mwa misinjeyo ndi wa madzi enieni opanda chosakaniza, wachiwiri ndi mtsinje wa mkaka weniweni opandanso chosakaniza, wachitatu ndi chakumwa cha ku Mparadiso, ndipo wachinayi ndi uchi wosasakaniza.

Kuli nyumba zazitali ku Mparadiso. Zimawerama, okhulupilira adzidzakwelapo ndipo azidzatengedwa kulikonse kumene afuna kupita. (Fanizo lake pa dziko pano ndi masitepe oyenda a ndege za makono.) Kuli mtengo wotchedwa ‘Tuba’ ku Mparadiso. Mizu ya mtengo umenewu ili mmwamba, ndipo nthambi ndi zophukira zake zalendewera mmunsi. Maonekedwe ake pa dziko lapansi ndi ngati mwezi ndi dzuwa.

Anthu aku Mparadiso amasangalala ndi kudya ndi kumwa ndipo amakhala okhutira ndi zakudya ndi zakumwazo; koma samamva nkodzo kapena kufuna kuchita chimbudzi; iwo ali kutali ndi zosowa ndi zowawa za umunthu zoterozo.

Allahu ta'âlâ adzawayankhula akapolo Ake, Okhulupirira ku Mparadiso kuti: **"E inu akapolo Anga! Mukufuna kuti ndikupatseninso chiyani? Pitirizani kusangalala ndi zosangalatsa ndi chitonthozo!"** Akapolo adzayankha kuti: "Ya Rabbi! Mwatimasula ku Jahannama ndi kutilowetsa ku Mparadiso Wanu, ndipo mwatipatsa akazi a ku Jannah ochuluka komanso ma ghilman ndi ma wildan. Ndizochititsa manyazi kwa ife kupempha zina." Pamenepo Rabb-al-alamin adzawayankhulanso nati: **"E, inu akapolo Anga! Pali chinthu china chomwe mudzapemphe kwa Ine, kuposa izi."** Akapolo akayankha kuti, "Ya Rabi! Tilibe khumbo lopempha zambiri. Komanso sitikudziwa chomwe tingapemphenso," Rabb-ul alamin adzawafunsa: **"E, inu akapolo Anga! Munkachita chiyani mutakumana ndi vuto pa dziko lapansi?**

Akadzayankha kuti amafunsa ma ulama (akatswiri a Chisilamu) ndipo vuto lawo limathetsedwa akaphunzitsidwa, Hadrat Haqq subhânahu wa ta'âlâ adzati: **"Chitani zomwezo tsopano ndipo dziwani pofunsa kwa ulama."** Choncho ma ulama adzati kwa okhulupilira: "Kodi mwayiwala za Jamalullah? Pamene munali pa dziko lapansi munkalakalaka mutamuona Allahu ta'âlâ ndi kunena: "Mmoyo omwe uli nkudza, Mbuye wathu, yemwe ali kutali ndi malo, Adzationetsa kukongola Kwake." Zimenezo ndi zomwe mungapemphe tsopano." Pamenepo adzapempha ruyat-ijamalullah (kuti awone Kukongola kwa Allahu ta'âlâ), ndipo Allahu adhîm-ush-shân.Waufulu ndi Wotalikirana ndi malo, adzawawonesa jamal-ibakamal Yake. Akadzaona jamal-al-pak ya Haqq ta'âlâ, kusilira kwawo kudzatha zaka zikwi zambiri.

Kudzakhala zipatso kuzungulira nyumba za okhulupirira ndi mmazenera momwe. Akangoganiza kuti, "Nditambasule dzanja langa ndikoke nthambiyo kuti ndithyole chipatsocho," sadzafunika kudzuka pa mpando wawo kuti akoke nthambiyo. Nthambi yomwe akufunayo idzayandikira yokha pomwe akhala iwo. Adzidzathyola chipatsocho nndi kuchiyika m'kamwa mwawo, ndipo kukoma kwake kusanafike kummero kwawo, chipatso china chidzakhala chitamera pomwe anathyola choyambapo. Akayika chipatso mkamwa mwake chidzakhala chakupsa komanso chokoma. Choncho, Rabb-ul-'izza adzalenga chipatso china cha tsopano.

Ngati muli ndi nzeru, chitani Swalah, poti ndiyo mapeto a chimwemwe.
Kuzindikira kwanu kwa Swalah kukhale kuti ndi Mi'raj kwa anthu Okhulupilira.

MAPEMPHERO OSACHITIKA M'NTHAWI YAKE (Swalah za Qada)

Swalah yochitika m'nthawi yake yodziwika yokhazikitsidwa ndi Imam wa mdera lanu imakhala ya phindu kwambiri. Zopindulitsa zina mwa izo zinanenedwa ndi akadaulo a Chisilamu ndi izi:

1- Ubwino woyamba ndi wakuti nkhope ya wopemphera idzakhala ya nur paliponse.

2- Moyo wa opemphera udzakhala ndi baraka.

3- Zopempha zomwe opempherayo wazitchula zimavomeredwa (ndi Allahu ta'âlâ).

4- Wochita Swalah adzakhala munthu wa khayr (wabwino).

5- Wochita Swalah adzakhala wokondedwa kwa okhulupilira onse.

Kupyonya Swalah popanda udhr iliyonse, kutanthauza kuswali swalah mochedwa popanda chifukwa chololedwa m'Chisilamu, kumadzetsa mavuto khumi ndi asanu (15). asanu mwa mavutowa amaoneka pa dziko la pansi pani; atatu mwa izo amachitika pa nthawi ya imfa; atatu m'manda; Ndipo anayi mwa iwo ali pa malo a Arasat.

Mavuta asanu pa dziko la pansi pano ndi awa:

1- Pa nkhope ya munthuyo sipadzakhala nur.

2- Sadzakhala ndi baraka m'moyo wake.

3- Mapemphero ndi zopempha zake sidzilandiridwa.

4- Madalitso amene wamfunira m'bale wake wa Chisilamu sangavomerezedwe ndi Allahu ta'âlâ.

5- Sadzalandira thawab pa mapemphero ake ena.

Mavuto atatu a pa nthawi ya sakarat-i-mawt (zowawa za pa nthawi yokumana ndi imfa) ndi izi:

1– Adzafa ndi njala.

2- Adzafa ndi ludzu.

3- Adzafa monyozeka. Chakudya ngakhale chochuluka bwanji sichingathetse njala yake kapena madzi a mtundu uliwonse sadzathesa ludzu lake.

Mavuto atatu a m'manda ndi awa:

1- Manda ake adzamufinya, kotero kuti mafupa ake adzathyokathyoka.

2- Manda ake adzakhala ndi moto paliponse.

3- Chinjoka chidzamugwera iye. Chinjokacho chimenechi chimatchedwa Aqra. Chidzatenga ndodo m'dzanja lake ndipo chikamenya munthuyo ndi ndodo yake, munthuyo adzidzamira mwakuya pansi pa nthaka kenako ndikubwereranso mmandamo. Ndipo njokayo idzidzabwereza kumenyako mpaka kufikira tsiku la chiweruzo. Kotero munthuyo adzazunzidwa mpaka tsiku la Kiyama.

Mavuto anayi a pa malo a Arasat ndi awa:

1- Adzadutsa mu chiweruzo chovuta kwambiri.

2- Adzakhala atadzisonkhezera mkwiyo wa Allahu ta'âlâ.

3- Adzalowa ku Jahannama.

4- Pa chipumi pake padzalembedwa mawu atatu:

Mawu oyamba adzati: Munthu uyu akuyenera mkwiyo wa Allahu ta'âlâ.

Mawu achiwiri adzati: Munthu uyu waonongo ufulu wa Allahu ta'âlâ.

Mawu achitatu adzanena: Popeza waonongera ufulu wa Allahu adhîm-ush-shân, uli kutali ndi Chifundo cha Allahu ta'âlâ.

Swalah ndiyo nsanamira yayikulu ya Chisilamu.

Ngati munthu akuswali Swalah zonse kasanu pa tsiku, iye adzakhala kuti wayimitsa nsanamira yayikulu ya chikhulupiliro chake. Potero adzakhala atamanga nthunzi wabwino okhalamo. Ngati munthu wasiya Swalah imodzi akuzindikira ndipo osachita qada (osabwezera nthawi ina), m'Madhhab onse atatu akugwirizana kuti fatwa idzaperekedwa kuti aphedwe. Malinga ndi Madhhab a Hanafi, sikofunika kuti aphedwe. Koma iye adzakhala kuti wachita limodzi la 'al-kabair' (machimo akulu). Kudzafunika (kumutsekera kundende) mpaka atayamba kuchita Swalah (mapemphero ake a tsiku ndi tsiku). Munthu wonyalanyaza Swalah chifukwa chakuti samayiwona ngati yofunikira komanso kuti sakhulupilira zoti Swalah ndi ntchito yoyambilira ya okhulupilira, iye adzakhala Kafiri (wosakhulupilira).

Ngati munthu aphonya Swalah imodzi mwa Swalah zisanu za pa tsiku mongofuna koma kenako ndikuchita Qada, iye adzasungidwa kumoto wa Jahannam kwa nthawi yotalikirapo yotchedwa 'huqba' ngakhale kuti walipira ngongole ya Swalah anaphonyayo. Huqba ndi zaka makumi asanu ndi atatu (80). Kuti akhululukidwe ku chilango

chimenechi, adzayenera kuchita tawba ndi kupempha chikhululuko. (Tsiku limodzi m'moyo winawo lidzakhala lofanana ndi zaka chikwi za padziko la pansi. Zaka za m'moyo winawo ziyenera kuwerengedwa pozindikira izi).

[Muhammad Amin Ibni Abidin "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" akunena m'bukhu lake lotchedwa **Radd-ul-muhtar**: Monga zanenedwera ndi akadaulo a Chisilamu, Swalah yakhala lamulo la chipembezo mu zipembedzo zonse zomwe zinavumbulutsidwa. Adam „alaihim-salâm" amaswali tsiku lililonse nthawi yamadzulo, Yaqub "alaihim-salâm" amaswali tsiku lililonse nthawi madzulo dzuwa likangolowa, ndipo Yunus "alaihim-salâm" amaswali tsiku lililonse nthawi usiku.

Ndi mfundo imodzi ya iman kukhulupilira ntchito za fardh kuti ndi Fardh ndipo ntchito za haram kuti ndi haram. Chimodzimodzi ndi mfundo ya iman kukhulupilira kuti ndi udindo wathu kuswali kasanu pa tsiku. Koma kuchita Swalah si nsanamira ya iman.

Ndi fardh kwa Msilamu wokwima nzeru ndi wa msinkhu, mamuna kapena mkazi, kuchita Swalah kasanu patsiku, pokhapokha ngati ali ndi 'udhr (chifukwa chovomerezeka chomulepheretsa kutero). Swalah kasanu pa tsiku zinakhala fardh mu usiku wa Mi'raj. Hadith-i-sharif ikugwira mawu a m'mabuku a **Muqaddima-us-salat, Tafsir-i-Mazhari** ndi **Halabiy-i-kebir** amene akufotokoza motere: **"Jebrail „alaihim-salâm"** ndi Ine tinachita Swalah limodzi ndipo Jebrail "alaihim-salâm" **ndiyemwe anatsogolera Swalah ngati imam wa a wirife, pafupi ndi khomo la Ka'ba, kwa masiku awiri otsatizana. Awirife tinaswali Swala ya m'mawa kukuyamba kuyera; Swalah yoyamba masana dzuwa litangosuntha pa liwombo; Swalah yachiwiri masana nthunzi wa chinthu uli wolingana ndi msinkhu wake nkuonjezerapo kutalika kwa chinthucho; Swalah yamadzulo dzuwa litangolowa,** [mbali ya dzuwa ya kumtunda itazimilirika;] **ndi Swalah ya usiku mdima utagwa. Tsiku lachiŵiri, tinaswali Swalah ya mmawa kuwala kwa dzuwa kutayamba kuonekera; Swalah yoyamba ya masana pamene nthunzi wa chinthu chinali chitatalika ngati kutalika kwa chinthucho; Swalah yachiwiri yam asana tinaswali titangoswali swalah yoyamba ya masana; Swala ya madzulo pa nthawi yoyikika yomasulira kusala; ndi Swala ya usiku kumapeto kwa gawo lachitatu la usiku. Kenako anati: 'Ee, iwe Muhammad, izi ndiye nthawi za Swalah** (mapemphero asanu apa tsiku) **kwa iwe ndi Atumiki omwe analipo iwe usanabwere. Ummat wako uchite Swalah iriyonse mwa Swalah zisanu izi pakati pa nthawi ziwiri zomwe tachita limodzizi.'"** Talamulidwa kuchita Swalah kasanu pa tsiku. Ndi udindo wa makolo kulamula mwana onse omwe

akwanitsa zaka zisanu ndi ziwiri (7) kuswali. Ndi kololedwa kwa bamboo kapena mayi kumenya mwana ndi dzanja amene sakuswali atakwanitsa zaka khumi. Ndi kosaloledwa kumenya wophunzira kupitilira katatu, kapena kumumenya ndi ndodo. Mwana aumirizidwa kusala (kufunga) ndipo amenyedwe ngati akukana kusala m'mwezi wodala wa Ramadan. Amenyedwenso pomuletsa kuti asamwe zoledzeretsa.

Munthu yemwe akukanira zoti kuswali fardh komanso kuti ndi ntchito yayambirira kwa Msilamu amakhala wosakhulupilira (kafiri). Ngati sakuswali chifukwa cha ulesi ngakhale akukhulupilira kuti swalah ndi fardh, amakhala Msilamu wa **Fasiq**. Munthu wotero atsekeredwa kundende mpaka atayamba kuchita Swalah. Izi zichitike mosanyengelera kapena kukhululuka. Ngati sayamba kuswali kasanu pa tsiku, amatsekeredwa ku ndende mpaka imfa yake. Akatswiri ena amati amenyedwa mpaka kutuluka magazi. Mu Madhhab a Shafi'i ndi Maliki, munthu amene wasiya Swalah imodzi sakhala kafiri, koma adzaphedwa monga chilango. Zanenedwa ndi akadaulo a m'Madhhab Hanbali kuti munthu wotere amakhala wosakhulupilira ndipo amaphedwa ngati chilango. Pali akatswiri ena omwe ali ndi ijtihad yofanana ndi yomweyi m'Madhhab a Shafi'i. Munthu akaswali pa jama'at, zimatengedwa kuti iye ndi Msilamu. Pakuti, nthawi zakale mmadera ena kunalibe Swalah ya jama'at; okhulupilira amaswali paokha. Kupembedza kwina komwe ankachita ndi Haji. Poti Swalah ndi kulambira komwe kumachitika ndi thupi la munthu yekha, ndi zosatheka munthu kuchita Swalah m'malo mwa wokhulupirira wina. Chifukwa choti Zakat ndi kulambira komwe kumachitika ndi chuma chokha, munthu ngakhala palibe udhr atha kuuza munthu wina kuti apereke zakat m'malo mwake pogwiritsa ntchito chuma cha olamulayo. Chifukwa choti Haji ndi kulambira komwe kumachitika ndi thupi komanso chuma, munthu amene ali ndi udhr (chifukwa chovomerezeka chomulepheretsa kupita ku Haji) akhoza kupempha munthu wina kukamuchitira Haji pogwiritsa ntchito ndalama zake, (ndalama za otumayo). Munthu wokalamba kwambiri amene sangathe kusala kudya kwa moyo wake wonse akhoza kupereka 'fidyah'[1] pa tsiku lililonse losala kwa Asilamu osauka.

Ndi kosaloledwa kulipira fidya m'malo mwa Swalah. Ngati munthu wolephera kuchita Swalah wafotokoza mu chifuniro chake chomaliza

[1] Fidyah ndi chopereka chomwe chimalipilidwa kwa osauka ndi munthu yemwe sangate kusala. Chimalipiridwa ngati munthu ali ndi chifukwa chokwanira chomilepheretsa kusala.

(will), ndi bwino akamwalira kulipira fidya pa ngongole zake zokhuza Swalah kuchokera mu chomwe wachisyya. Ngati chuma chimene wasiya sichikukwanira pa isqat, zikuloledwa kuchita **dawr**. Koma kusala kudya, kuli wajib kuchita isqat.

M'nyengo ya chilimwe m'maiko akumpoto, kumalo komwe fajr imayamba mdima usanakwanire kwenikweni, kutanthauza kuti nthaŵi za mapemphero a usiku ndi mapemphero a m'maŵa sizioneka bwino, sikoyenera kuswali mapemphero awiriwa, malinga ndi Madhhab a Hanafi.

Mujtahid wamkulu, Imam Shafi'i "rahima-hullâhu ta'âlâ" anatulutsa ijtihad kuti mapemphero awiriwo ayenera kuchitika. Koma malinga ndi akadaulo ambiri a Chisilamu, anthu omwe akukumana ndi zomwe tafotokozazi, sayenera kupemphera m'mawa ndi usiku. Koma sakuyenera kuchita Qada. Pakuti, nthawi zoyikidwiratu za Swalah iliyonse siyinayambe, Si fardh kuchita Swalah yomwe nthawi yake siyinakwane. Koma izi siziri choncho ndi kusala kudya. Mwezi watsopano ukawoneka m'dziko limodzi, Ramadan imayambika m'maiko onse.

Ngati mukumana ndi haraj pamene mukuchita chinthu cha fardh kapena kupewa kuchita chinthu cha haram, muyenera kutsanzira Madhhab ena, imodzi mwa Madhhab ena atatu, omwe mulibe haraj imeneyo. Haraj ikutanthauza kuchita chinthu movutikira kapena kulephera kuchita kumene. Ngati palibe imodzi mwa ma Madhhab atatuwo yomwe ili yomasuka ku haraj imeneyo, ndipo ngati haraj ikupezeka chifukwa cha darurat,[1] mukhululukidwa kuchita fardh kapena kupewa haram imeneyo. Koma ngati haraj ilipo popanda darurat, ndiye kuti muyenera kuchotsa harajyo mwanjira inayake popanda kuthana ndi chomwe chinayambitsa.

Msilamu amene wachedwa ku Swalah ya m'mawa asiye sunnah kuopa kuti angaphonye gawo la Swalah ya m'mawayo mu jama'at. Ndi koyenera kwa iye kusiya Sunnah kuopera kuphonya nthawi ya Swalah ya m'mawa. Ngati akuona kuti atha kuyipeza Jama'at, Sunnah akaswalire kunja kwa Msikiti kapena kuseri kwa mizati umodzi mkati mwa mzikitimo. Ngati palibe malo abwino ochitira sunnah, ayenera kusiya Sunnah koma asa chita pafupi ndi Asilamu omwe ali pa jama'at.

[1] Darurat ndi samavi (mwakusafuna) chomwe chimakukakamizani kuchita chinthu kapena chomwe chimakulepheretsani kupewa china chake, vuto lomwe lingachitike loti simungalipewe.

Pakuti kuchita Sunnah kuyenera kusiyidwa ndi cholinga chopewa kuchita makruh.

Swalah za Fardh zomwe zaphonyedwa pa chifukwa chovomerezeka (udhr) zimatchedwa **fawait**, kutanthauza kuti Swalah za fardh zomwe mwalephera kuchita mu nthawi zake. Swalah zomwe zaphonyedwa chifukwa cha ulesi komanso popanda udhr zimatchedwa **metrukat**, kutanthauza kuti zomwe zasiyidwa popanda udhr. Akatswiri a Fiqh amazitcha **fawait** Swalah (zosachitika chifukwa cha udhr ndi) kusiyidwa mpaka qada mmalo mozitcha Swalah zophonyedwa.

Pakuti, ndi tchimo lalikulu kusachita Swalah mu nthawi yake yoyikidwa popanda udhr. Tchimo limeneli silingakhululukidwe pochita qada pokha. Kuonjezera apo, ndi kofunika kuchita tawba ndi kuchita hajj-i-mabrur. Qada ikachitika, kuti Swalah yosiyidwa yachitika ndi kulipidwa ngongoleyo, tchimo lomwe lakhululukidwa ndi lokhalo lophonyetsa Swalah ndikusayichita mu nthawi yake. Tawba yochitika popanda kuchita qada, popanda kubweza ngongole siidzakhala sahih. Siidzakhala tawba yovomerezeka, Pakuti, tawba yochitika chifukwa cha tchimo imadalira pa kusiya kuchita tchimo lokhudzidwalo.

Pali ma udhr asanu (zifukwa zomveka zololedwa ndi Chisilamu) zochedwetsera Swalah mpaka nthawi yake kutha: Munthu woti akulimbana ndi mdani sangathe kuchita Swalah chokhala pansi kapena kutembenukira ku Qibla kapena kukwera pa nyama; Musafir (wa pa ulendo wautali wotchedwa 'safar'), ali pa chiwopsezo chogwidwa ndi akuba, achifwamba kapena zilombo pa njira; Mzamba yemwe akuona kuti pali chiwopsezo choti mayi kapena mwana akubadwitsa angathe kufa; Ndi udhr kwa anthu atatu (awa) kuchedwetsa Swalah zawo. Udhr yachinayi ndi kuyiwala, ndipo yachisanu ndi kugona. Swalah idzawerengeredwa kuti yachitika mu nthawi yake (ada)[1] mu Madhhab a Hanafi ngati opempherayo atakwanitsa kuchita takbir iftitah, ndipo m'Madhhab ya Shafi'i, ngati atakwanitsa kuchita rakat imodzi (ya Swalah), nthawi yake yoyikika isanathe.

Ndi fardh kuchita qada Swalah zomwe ziri fardh, komanso ndi wajib kuchita qada Swalah za wajib. Ngati munthu achita qada Swalah ya Sunnah, adzapeza thawab za Swalah ya Sunnah. Ndikoyenera kutsata ndondomeko ya kachitidwe ka ada ya zigawo za fardh ndi witr za Swalah zisanu za pa tsiku komanso pochita qada ya Swalah

[1] Kuchita ada ya Swalah ina yake kumatanthauza kuyichita mkati mwa nthawi yoyikid-wiratu. Kuchita qada kumatanthauza kuichita Swalah nthawi yake itatha

zimenezi. Lamuloli siligwira ntchito pamene nthawi yopemphera ikucheperachepera. Mwachitsanzo, Swalah yanthawi imeneyo isasiyidwe ndi cholinga chofuna kuchita qada ya Swalah yomwe nthawi yake yapita. Choletsa china cha lamuloli ndi chakuti mungayiwale kuti muli ndi ma faita Swalah, (Swalah zomwe munaphonya, kapena kuchuluka kwa ma faita Swalah akhala asanu ndi imodzi.

Tertib, (mdandanda wa kapempheredwa ka swalah za pa tsiku) siungalongosokenso ngati Swalah zoyenera kubweza sizikukwana zisanu ndi imodzi (6). Ngakhale kuti Swalah za fardh zoswali mosalabadira tertib zidzakhala fasid, (sidzizavomerezeka,) koma ngati Swalah zakwana zisanu ndi imodzi zonse zidzakhala sahih (zovomerezeka) ikangotha nthawi ya Swalah ya chisanu. Mwachitsanzo, tiyerekeze kuti munthu sanaswali Swala ya m'mawa (Fajir) koma waswali swalah yoyambilira masana (Dhuhr), yachiwiri yamasana (Asr), ya madzulo (Maghrib), ya usiku (Eisha) ndi witr (koma osati Swala ya m'mawa) ngakhale akukumbukira kuti sadaswali m'mawa; Swalah zonsezi palibe imene ikhale sahih, koma onsewo adzakhala Sahih likatuluka dzuwa (m'mawa mwake).

Faita Swalah (swalah zophonyedwa) ziyenera kubwezeretsedwa mwachangu.

Ndikololedwa kuchedwetsa mpaka mutapeza zofunika pa moyo wa banja lanu ndikuchita gawo la Sunnah ya Swalah zisanu za tsiku lirilonse ndi Swalah zotchedwa duha ndi tasbih ndi tahiyyat-ul-masjid. Ibni 'Abidin akunena motere m'gawo limene akufotokoza za ma sunnah a udhu kuti: "Zololedwa' zikutanthauza 'Zosaletsedwa'. Mchitidwe womwe ndi makruh tanzihi ukunenedwa ndi akadaulo a Chisilamu kukhala 'wololedwa'." Ndi kofunika kusachita zinthu zomwe zimanenedwa kuti ndi 'zololedwa (jaiz)', koma qada ya Swalah isamachedwetsedwe chifukwa chochita ma Sunnah a Swalah. Qada ya masiku omwe mwalephera kusala mu Ramadan sichinthu choti muchite mwachangu.

Munthu yemwe walowa Chisilamu mu Dar-ul-harb (dziko la anthu osakhulupilira) sayenera kuchita qada ya Swalah, kusala kapena kupereka zakat zomwe sadachite mu nthawi yake chifukwa samazidziwa. Koma kusadziwa zinthu zomwe ziri fardh ndi zomwe zili haram si udhr kwa anthu okhala mu Dar-ul-islam (mdziko la Asilamu). Ngati murtadd, (wopatuka amene wasiya Chisilamu) abwerela ku Chisilamu, sayenera kuchita qada ya Swalah zomwe sanaswali pa nthawi ya mpatuko wake. Pakuti, Chisilamu sichimawauza zochita anthu osakhulupilira. Ngati sabi, (mwana wosatha msinkhu komanso

amene sali woyenelera pa malamulo a Chisilamu), waswali Swala ya usiku kenako ndi kukagona, ndikuzilotera atagona usikuwo ndi kudzuka pambuyo pa fajr (m'bandakucha) m'mawa wa tsiku lotsatiralo, iye ayenera kuswali Qada ya Swalah ya usiku wapitayo. Pakuti Swalah yomwe anachita usiku wapitawo inali nafila (Sunnah), ndipo inadzakhala fardh kwa iye atagona.

Ngati pali Swalah zomwe munaphonya munali a thanzi, ndi kololedwa kuzichita qada ndi tayammam ndi ima pamene mukudwala. Swalah ya ma rakat anayi yomwe yasiyidwa ku qada iyenera kuchitidwa qada ndi ma rakat onse anayi ngakhale muli pa safar (ulendo wautali). Ma rakat anayi a fardh a swalah yoyamba yam asana (dhuhr) yomwe yaphonyedwa muli pa safar (ulendo wautali) ayenera ku swalidwa popanga qada ndi ma rakat awiri ngakhale mutakhala muqim (mutafika komwe mumapita). Poyamba Swalah ya Fardh yoyamba ya masana chitani niyya kuti mukuchita fardh ya "Swalah ya lero ya masana, kapena, "kuchita fardh ya swala ya masana." Ngati pali faita Swalah zoposa imodzi chitani niyya yanu mu mndandanda wake monga kunena motere: "Qada ya Swalah ya dhur yomwe inasiyidwa," kapena "Qada ya swalah ya fardh Asr," pamene (mukuyamba) kuchita qada iliyonse. Koma pochita ma Qada ya kusala kwa masiku ophonyeka a Ramadan sikoyenera kutsata dongosolo la nthawi pakati pawo.

Pochita qada ya Swalah zomwe munasiya popanda chifukwa (udhr) zomwe zimatchedwa metruk, musawuze anthu ena. Chifukwa, ndi tchimo lalikulu kusachita Swalah mu nthawi yake yoyikika. Ndi tchimo linanso kudziwitsa ena za tchimo lanu. Utchimo wina ndi kuwuza ena masana za machismo omwe mwachita usiku watha. Apa tamalizitsa kumasulira kwathu kuchokera mu Ibni Abidin.

Monga tawonera, m'Madhhab a Hanafi ma Faita Swalah ayenera kubwezedwa pochita qada mwachangu. Lamuloli ndi chimodzimodzi m'Madhhab a Shafi'i. Shams-ud-din Muhammad Ramli "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", katswiri wa Chisilamu m'Madhhab a Shafi'i, akunena motere m'buku lake la ma fatwa: "Ngati munthu ali ndi Swalah zomwe sanachite chifukwa cha udhr, sitchimo kwa iye kuchita Swalah yotchedwa Tarawih mu Ramadan ndi kuchita qada ya Swalah za faita Ramadan itatha. Koma ndi kulakwa kwa munthu amene waphonya Swalah popanda udhr kuchita chimodzimodzi. Kwa iye Swalah zophonyeka ziyenera kuzichita qada mwansanga."

Akatswiri a Chisilamu a Madhhab a Shafi'i akunena poyera kuti ndi tchimo kuchita Swalah za Sunnah monga tarawih m'malo moyamba

kuchita Swalah zosiyidwa popanda udhr. Lamulo lomweli likugwiranso ntchito m'Madhhab a Hanafi. Lamulo la Madhhab a Hanafi loti ndi kololedwa kuchedwetsa qada ya Swalah za faita chifukwa cha 'udhr, ndi chisonyezo chakuti ndi bwino osachedwetsa kuchita qada. Poti kuloledwa (jaiz) kukutanthauza kuti zosaletsedwa. Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akufotokozera mauwa, "...zololedwa (jaiz) kugwiritsa ntchito madzi oyenda moononga" pomwe ndi "makruh tanzihi...." Pamene kuli kwa bwino kuchita changu pochita qada Swalah zophonyadwa chifukwa cha udhr, ndi kokakamizidwa kuchita Swalah zosiyidwa popanda udhr m'malo mochita ma Sunnah za Swalah zisanu. Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akunena kuti: "Pochita udhu, ndi Sunnah-i-muakkada kusambitsa chiwalo chilichonse choyenera kusambitsidwa pa udhu katatu. Si makruh kusiya Sunnah imeneyi ngati pali udhr monga; kukwera mtengo wa madzi, kuzizira kwa madzi, ndi kusowa kapena kuchepa kwa madzi." Ichi ndi chizindikiro china choti utha kuthana ndi utchimo waukulu pochita qada ya Swalah zosiyidwa, ndi kofunikanso kuchita qada ya Swalazo m'malo moswali Sunnah za Swalah zisanu za pa tsik, kupatulapo swalah ya m'mawa. [Momwe mungachitire qada Swalah m'malo mmalo mwa Sunnah zafotokozedwa kumapeto kwa mutu wonena za Kufunika kwa Swalah.]

KUWOMBOLA WOMWALIRA KU NGONGOLE ZA SWALAH

[Isqat ya Swalah ikutanthauza 'kupulumutsa omwalira ku ngongole zake za Swalah'. Pochita izi, kaffarah ya Swalah zake zomwe anaziphonya kapena kuzisiya zimalipidwa. Kuti kaffarat ilipiridwe, zimzkhala wajib ngati womwalirayo analamula mu wilo yake kuti zizachitike ndipo kuti wasiya chuma chokwanira chodzachitira izi.

Gawo limodzi mwa magawo atatu (⅓) ya chuma chimwe wasiya chikhale chosachepera chuma chofunika kuchitira kaffarat. Kaffarat amalipira ndi wali wa womwalilayo, yemwenso amakhala munthu wapatsidwa udindo wosamalira chuma cha masiye, kapena m'modzi mwa olowa mmalo mwa omwalira.

M'Chisilamu muli ma Wali a mitundu inayi: Wali wa mayyit (wa womwalira), wali wa yatim (amasiye) wali wa mkazi yemwe anali naye pa mgwirizano wa ukwati (nikah), uyenera kuchitika; ndi wali wa kapolo kapena jariya. Mtundu wotsiriza wachinayiwu umatchedwanso **mawla**. Palinso ma Wali ena kupatula pa ma wali anayiwa: Ma wali a

Allahu ta'âlâ omwenso amatchedwa **Awliya.** Awa ndi anthu amene Allahu ta'âlâ amawakonda kwambiri. Kupeza chikondi chozama ngati ichi kumafunika kukhala ndi zoziyenereza zonse zokhudzana ndi mawu, zochita, ndi chikhalidwe chabwino komanso kuphunzitsidwa ndi Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam". Maphunziro amenewa atha kupezeka mosavuta kuchokera kwa akadaulo a Chisilamu eni-eni. Munthu amene sangathe kupeza kadaulo wa Chisilamu aziphunzira kuchokera m'mabuku olembedwa ndi akadaulo a Ahl-as-Sunnah. Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akunena kuti: "Ngati munthu amene ali ndi faitas (Swalah zomwe anaphonya pali udhr [chifukwa]) wamwalira ndipo walamula mu wilo yake yomaliza kuti kaffarat ichitike, theka la 'saa' [malitala 2.1], kapena ma dirham 520 [1750 gr] a tirigu kapena ufa wa tirigu ziyenera kuperekedwa kwa osauka pa Swalah iliyonse yomwe ili fardh kapena wajib.

Zonsezi zikhoza kuperekedwa kwa munthu mmodzi wosauka. Ndibwino kulipira izi molingana ndi mtengo wa [golidi kapena siliva]. Ngati wopereka sanasiye chuma chilichonse kapena ngati gawo limodzi mwa magawo atatu (⅓) a chuma chimene wasiya sichikukwana kulipira kaffarat, kapena ngati womwalira sanasiye wilo, ndipo wali wake adzachita kaffarat yake popereka ndalama zochepa, iwo amabwereka zokwanira chaka. Popeza zofunikira patsiku ndi: 1750 x 6 = 10500 gr. kapena ma kilogalamu khumi ndi theka [10.5] a tirigu, iwo amabwereka mtengo wa chaka (masiku 360 [10500 x 360=3780000/1000]) = 3780 kg ya tirigu kapena -poti mtengo wa ma kilogalamu khumi ndi theka a tirigu nthawi zonse umakhala pafupifupi gramu imodzi ya golidi; kobidi la golidi zolingana pa mtengo wake, ndiye kuti 52.5 makobili a golide, kapena makobidi 60 a golide, chifupi chake, kapena zinthu zopangidwa ndi golide zolemera [432 gr] monga mphete, zibangiri ndi zina zotero. Poganiziranso kuti ndi kotheka kuti Swalah zomwe ankachita womwalirayo zinali ndi zolakwika, amachotsera zaka za ku ubwana wake motere: zaka khumi ndi ziwiri akakhala mamuna, ndi zaka zisanu ndi zinayi akakhala mkazi, ndipo potero amapeza chiwerengero cha zaka zonse zomwe malemuyo anali mukallaf, (woyenelera kuchita Swalah). Poti Swalah za pa tsiku zomwe kaffarat imafunika kulipira ndi zisanu ndi chimodzi (6), amabwereka [ma kg 3780] a tirigu, kapena ndalama za golide makumi asanu ndi limodzi (60), -kumene kuli kusankha kwa bwino; - zomwe zikufunika pa kaffarat ya Swalah za chaka chonse. Izi amazipereka kwa Msilamu wosauka pamene akuchita niyyah yake kuchita isqat ya kaffarat ya Swalah za mayyit (womwalira). Wosaukayo ayenera kukhala wozindikira, wotha msinkhu, Salih (wopembedza) ndi Msilamu

wachimuna. Munthu wosauka ameneyu anene, “Ndachivomera,” ndikulandira. Kenako munthu wosaukaye apereke kwa mulowa mmaloyo ngati mphatso. Mulowa mmalo uja amalandira ndikudzazipereka kwa wosauka yemweyo kapena wosauka wina.

Izi zimabwerezedwa kangapo chaka ndi chaka malinga ndi zaka zomwe mayyit anali mukallaf (anayenera kuchita Swalah). Ngati golide wobwereka ndi wochuluka kuposa Chitsanzo chenicheni chiwerengero cha ma dawrs (kubwereza) komwe kuyenera kuchitika kudzasintha m’chiŵerengero. Ngati ndalama za golide palibe, ‘wali’ amabwereka zodzikongoletsera za golide monga zibangili ndi mphete kuchokera kwa mzimayi, naziyeza pa sikelo ndi kupatula (zaka zomwe sanachite Swalah x 7.2g) ndi kuyika ndalama zolekanitsidwazo mu mpango, kotero kuti mukhala ndalama za golide zochuluka monga zaka zomwe malemuyo sanachite Swalah. Chiwerengero chichulukitsidwa ndi makumi asanu ndi limodzi [x60] ndipo zotsatira zake zidzagawidwa ndi kuchuluka kwa anthu osauka omwe akutenga nawo mbali mu dawr ndipo zidzapereka kuchuluka kwa ma dawr (kubwereza) koyenera kuchitika. Ngati golideyo ali wocheperako, theka la golide tatchula kale lija limayezedwa. Kuchuluka kwa ma dawr kudzakhala kawiri chiwerengero chochitika mu zomwe takamba kale. Tiyerekeze mamuna wamwalira ali ndi zaka makumi asanu ndi limodzi (60), tidzawerengera motere: 60 x 48 x 7.2 = 20736 gr ya golide idzapatsidwa kwa wosauka mmodzi. Tikutero chifukwa isqat ya Swalah ya chaka chimodzi mtengo wake ndi ma kobili a golide makumi asanu ndi limodzi [60]. Ma dawr makumi atatu [30] adzapangidwa ndi 100 gr ya golide ndi osauka asanu ndi awiri. Kapena ma dawr 43 adzapangidwa ndi 70 gr. ya golide ndi osauka asanu ndi awiri. Kutha apo ma dawr adzachitika a kusala chakudya, Qurban ndi kulumbira. Ndikofunika anthu osauka osachepera khumi pa kulumbira dawr, ndipo munthu m’modzi sangapatsidwe kupyola theka la ‘sa’ pa tsiku, pomwe munthu mmodzi akhoza kulipidwa ma kaffarah a Swalah zambiri pa tsiku limodzi, ndinso nthawi imodzi. Isqat ya zakat siyingachitike ngati malemuyo sanalamulire mu wilo yake. Malemuyo ayenera kulamula mwa chifuniro chake. Koma popeza kuti lamuloli siligwira ntchito pa kusala kudya, wali ayenera kuonanso zakat popereka kuchokera ku chuma chake. Ma dawr akatha, mulowa mmalo amapereka katundu kapena ndalama ngati mphatso kwa anthu osauka omwe anatenga nawo gawo mu dawr.

“Ngati gawo limodzi mwa magawo atatu a chuma chosiyidwa ndi womwalira yemwe analamula kaffarah m’chilamulo chake

sichikukwanira kuti achite kaffarah, wali (muyang'aniri) sangachite kaffarah powononga ndalama zoposa gawo limodzi mwa magawo atatu popanda chilolezo cha olowa mmalo. Ngati gawo limodzi mwa magawo atatu likukwanira kaffarah koma womwalirayo ali ndi ngongole, yambani kulipira ngongole musanachite kaffarat ngakhale mwini ngongole atapereka isqat. Wobwereketsayo akalipidwa zake, sangapereke (kubweza) ngati mphatso kuti kaffarah ithe kukwaniritsidwa.

Poti kukwaniritsa kwa kaffarah kudzakhala kovomerezeka ndi chuma chokhacho chomwe chaperekedwa ndi mulowa mmalo. Ngati womwalira alamula kaffarah pa Swalah za moyo wake wonse mu wilo yake, koma ngati sizikudziwika kuti anakhala zaka zingati, gawo la wilo yake limenelo lidzakhala batil (lopanda pake. Koma ngati gawo limodzi mwa magawo atatu liri locheperapo poyerekeza kuchuluka kwa Swalah za m'moyo wake wonse, ndipo analamula kuti gawo limodzi mwa magawo atatu onse aperekedwe, pamenepo gawo la wilo lidzagwira ntchito poti lanena kuchuluka kwake, motero (gawolo la) wilo yake likhala Sahih (lovomerezeka).

"[Ngakhale womwalirayo atalamula mu wilo yake kuti kaffarat ichitike, si wajib kwa wali, [yemwe ndi mulowa mmalo kapena wasi (woyang'anira),] kupereke mphatso kuti kaffarah ichitike. Ndi wajib kwa malemuyo kusiya chuma chokwanira chomwe gawo limodzi mwa magawo atatu la chuma chake lidzakwanira kaffarah zake ndipo alamule mu wilu yake kuti gawo limodzi mwa magawo atatuwo a chumacho achitire kaffarah. Ngati alamula kuti kaffarah ichitike ndi gawo limodzi mwa magawo atatu, ndipo lotsalalo liperekedwe kwa alowa mmalo ake kapena kwa anthu ena, ndiye kuti wapyola wajib, lomwe ndi tchimo. Pachifukwa chimenecho, sikuli sahih kulamula kuti gawo limodzi mwa magawo atatu agwiritsidwe ntchito pochita khatm a Qur'an al-kareem ndi tahlils (Itima). Kuonjezera apo, nkosaloledwa kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem kuti mulandire malipiro. Onse, olipira ndi olandira adzakhala wotchimwa. Ngakhale zanenedwa ndi akatswiri ena kuti ndikololedwa kulipiritsa maphunziro a Qur'an al-kareem, palibe katswiri ndi m'modzi yemwe wanena kuti ndi kololedwa kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem pofuna malipiro.

"Ngati munthu womwalira analamula mu wilo yake kuti Swalah zake zimene sanachite zichitike ndi mlowa m'malo wake, sikoyenera kuti mulowa mmalo achita qada ya Swalah za wakufayo. Koma ndi zololedwa kuchita Swalah kapena kusala ndikupereka thawab zomwe

amapeza ngati mphatso kwa wakufayo. Ndi kosaloledwa munthu yemwe akumwalira kulipira fidya pa Swalah zake." Apa tikumaliza kumasulira kwathu kuchokera kwa Ibni Abidin.

Ahmad Tahtawi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" akunena mu ndemanga yake ya bukhu lotchedwa **Meraq-il-felah:** Zanenedwa mu Nass, (zomwe ndi ayati karima ndi hadith-i-sharif zomveka bwino), kuti ndi kuyenera kuchita isqat pa kusala kudya komwe kunakanika m'nthawi yake polipira fidya mmalo mwake. "Popeza kuti Swalah ndi yofunika kwambiri kuposa kusala kudya, lamulo lomweli limagwiranso ntchito pa Swalah," awa ndi mawu omwe akadaulo a Chisilamu anagwirizana.

Choncho kunena kwa munthu wa cchipembezo kuti, "Isqat ya Swalah ndi chinthu chopanda maziko," ndi umbuli waukulu. Ndi mawu otsutsana ndi ndi zomwe akadaulo ophunzira za chipembedzo anagwirizana.

Ngati munthu wodwala akulephera kuchita Swalah ngakhale pochita zisonyezo ndi mutu wake pomwe wagona, sangalamule mu izo mu wilo yake ngakhale Swalah zimene sangachite za pa tsiku zili zochepera. Chimodzimodzi, ngati munthu walephera kusala chakudya chifukwa cha ulendo wautali kapena matenda, sangapeze nthawi ya Iqamah, (kukhazikika pamalo) kapena kukhala ndi umoyo wabwino kuti athe kupeza qada ya ngongole zosala, iye sayenera kulamula za isqat yawo mu wasiyyah yake.

Wasiyyah, ndi yothekanso pa sadaqa-i- fitr (yomwe siyinaperekedwe ndi omwalira), njira zopezera ndalama za mkazi, zolakwa zomwe anachita atatenga ihram yopita ku Haji, zachifundo zokhudzana ndi zopereka za malonjezo. Ngati munthu wamwalira osasiya wasiyyah, ndizololedwa inshaallah, kwa mlowam'malo wake kapena munthu wina aliyense kuti amuchitire. Ngati munthu wakufa walamula Haji mu wasiyyah yake, wakil (mulowa mmalo) wake apite ku Hajj kuchokera ku mzinda wa malemuyo kapena kuchokera pa malo pomwe gawo limodzi mwa magawo atatu a chuma chimene adasiya angakwanitse, koma wopita ku hajjiyo ali ndi mwayi wosankha malo ochokera popita ku Haji. Sizili sahih kwa aliyense kusala kapena kuchita Swalah m'malo mwa munthu womwalirayo, kaya polipidwa kapena mwaulere. Hadithi sharif yokhudza nkhaniyi ndi mansukh.[5] Chifukwa cha sadaka zoperekedwa monga kaffarat, Allahu ta'âlâ adzakhululukira ngongole za wakufayo (zokhudzana ndi zopembedza). Zanenedwa m'bukhu la Shafi'i lotchedwa, Anwar: "Si wajib kwa omwalira kulipira Fid'ya za Swalah zomwe sanachite. Ngati zalipiridwa

sidzizakhala isqat. Asilamu m'Madhhab a Maliki kapena Shafi'i amachita dawr potsanzira Madhhab a Hanafi.

Ngati kuchuluka kwa chuma chomwe womwalirayo analamula mu wasiyyah yake sichikukwanira pa kaffarat kapena ngati gawo limodzi mwa magawo atatu a chuma chomwe anasiya sichikukwanira kapena ngati wamwalira osasiya wasiyyah yake, dawr imapangidwa kuti isqat ya ngongole zake zonse zidzakwaniritsidwe ndi katundu ochepa woperekedwa ndi wina wake.

Zochepazi zimaperekedwa kwa munthu wosauka ndi cholinga cha isqat. Wosauka ameneyo, akadzalandira adzazipereka ngati mphatso kwa wali kapena kwa wosauka wina, amene nayenso ayenera kulandira mmanja mwake kenako amazipereka kwa wosauka wina ngati chopereka ndi cholinga cha isqat ya ngongole ya wakufayo (zopembedza monga Swalah ndi kusala kudya). Apa tamalizitsa kumasulira kwathu kuchokera kuzofotokoza kwa ndemanga za Tahtawi.]

SWALAH YA TSIKU LA CHISANU

Kuti swala ya tsiku Lachisanu ikhale sahih pakufunika kuti zinthu zisanu ndi ziwiri zikwaniritsike:

1- Malo omwe (wotchedwa mzinda) Swalah ya la chisanu iyenera kuchitikira ku omwe akulu.

2- Kuchita ulaliki wosanjidwa bwino wotchedwa khutba.

3- Kuyamba kuchita khutba musanachite Swalah.

4- Payenera kukhala Imam kapena Naibi (kuchokera ku boma) wophunzira bwino.

5- Kuti Swalah ya Jumu'ah ichitike mu nthawi yoyikika ya Swalah yoyamba ya masana (Dhur).

6- Pakhale Jamaat. Payenera kukhala gulu la anthu oti achite jama'at [kusonkhana pamodzi kwa Asilamu], pakuti, Swala ya la chisanu iyenera kuchitika pa jama'at.

Malinga ndi Imam A'zam ndi Imam Muhammad "rahima-hullâhu ta'âlâ!", Kupatula imam, payenera kupezeka amuna atatu owonjezera omwe ayenera kukhala amuna wokwana zaka za kutha msinkhu ndi wozindikira. Ndipo akachepetsetsa pakhale amuna awiri kuphatikiza imam, malinga ndi Imam Abu Yusuf "rahima-hullâhu ta'âlâ!". Qawl ya Tarafayn ndiyofunikira. (Imam A'zam Abu Hanifa ndi wophunzira wake wodalitsika Imam Muhammad amatchedwa 'Tarafayn'.)

7- Pakhale ufulu woti anthu apite kukasonkhana nawo kumapemphero a Lachisanu.

Zanenedwa motere m'bukhu la fatwa lotchedwa **Hindiyya**: “Ndi fardh ayn kwa amuna omwe ndi afulu, athanzi komanso sali safari kuswali Swala ya Jummah. Sizili fardh kwa munthu wayenda ulendo wautali wotchedwa safar kapena wofowoka kapena kwa akazi kuswali swala ya la chisanu. Si fardh ngakhale kwa amuna omwe sangatuluke powopa kupezeredwa ndi mvula yamkhuntho kapena kuyimbidwa mulandu ndi akuluakulu aboma. Mabwana, atsogoleri ngakhale olemba anzao ntchito asaletse anthu omwe akuwayang’anira kukachita swalah ya la Chisanu. Akhoza kudula malipiro ngati akuwona kuti ndikofunika kutero.

Ngati imam otsogolera Swalah ya Jumu'ah ali fasiq ndipo simungathe kumuletsa, malangizo a ukadaulo ndiwoti pempherani kumbuyo kwake osati kusiya Swalah ya Jumu'ah. Koma nthawi zina monga mapemphero asanu a pa tsiku pitani ku mzikiti komwe imam wa Salih akutsogolera Swalah ya jama’at mmalo moswali potsatira imam wa fasiq. Ndi makruh kwa mkazi kupita ku mzikiti ndi cholinga chokachita Swalah pa jama’at, posatengera kuti mkaziyo ndi ndani komanso kuti Swalah yoti achite ndi yotani.]

Malinga ndi Imam Muhammad “rahima-hullâhu ta’âlâ!”, munthu yemwe wapeza imam ali pa Ruku ya raka'at ya chiwiri ya Swalah ya Jumu'ah, ayenera kuswali Swalah yoyamba ya masana ya pa tsiku (Dhur). Koma Imam Azam ndi Imam Abu Yusuf “rahima-hullâhu ta’âlâ!”, akuti ayenera kuswali Swalah ya Jumu'ah ngakhale atamupeza imam mochedwa ali pa tashahhud (atakhala pansi). Ngati munthu akuchita nafila (Swalah yapadera), Khatib[1] ndi kuyamba kunena kapena kuwerenga khutba, iye ayenera kuswali ma rakat awiri okha, osapitilira pamenepo. Koma ngati akuswali Sunnah (yoyamba) ya Swalah ya Jumu'ah, akatswiri a Chisilamu sanagwirizane zoti aswali ma rakaat awiri ndikupereka kaye salaam, kapena kuswali rakaat zonse zinayi. Koma ndi kofunikira, kuswali rak'at zonse zinayi.

Pali ma wajib asanu omwe ayenera kutsatidwa la Chisanu:

1- Kuyimitsa ntchito za mtundu uliwonse pa nthawi ya Adhan ya (mapemphero a masana).

2- Kupita ku mzikiti poyenda mofulumira ngati kuyenda komwe kumatchedwa 'saai' (kuyenda mwachangu monga momwe amachitira poyenda pakati pa mapiri otchedwa Safa ndi Marwa pa nthawi ya Haji.

[1] Khatib ndi yemwe akuwerenga kapena kupereka khutuba pa tsiku la Jummah

3- Osaswali Swalah ya nafila ngati imam akuchita khutba.

4- Kupewa zokamba za dziko.

5- Kukhala chete.

Pali mustahab asanu ndi imodzi omwe ayenera kutsatidwa pa rsiku lachisanu:

1- Rayiha-i-tayyiba, (kudzithira kapena kudzipopera mafuta onunkhira.)

2– Kugwiritsa ntchito miswak, (yomwe ndi nthambi ya m'mtengo araq.)[1]

3– Kuvala zovala zoyera (zopanda nyansi).

4- Tabkir, [kupita ku mzikiti molawilira kukapemphera Jummah. Munthawi ya Zaman- Sa'adat, ma Khalifa a Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" oyambilira anayi, samabalalika akatha Swalah ya m'mawa la Chisanu. (Zaman- Sa'adat ndi nthawi yodalitsika ya chisangalalo yomwe Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anali ndi moyo ndi ma Khalifa ake oyambilira anayi awa: Hadrat Abu Bakr, Hadrat Umar, Hadrat Uthman ndi Hadrat Ali "radiyallâhu 'anhum ajma'in"). Iwo amabalalika ataswali Swala ya Jummah. Chomwe Ummat uwu wa Asilamu unachinyalanyaza poyamba, linali khalidwe lomwe ndi Sunnah ndipo limatchedwa tabkir.]

5- Kuchita ghusl

6 – Kunena pemphero lotchedwa Salawat, (lomwe limatchulidwa pa mzimu wodala wa Mtumiki wathu "sallallâhu alaihi wa sallam" ndipo limati: **"Allahumma salli 'ala sayyidina Muhammadin wa 'ala [alihi wa sahbihi] ajma'in."**)

Pali makruh asanu oyenera kupewa pa tsiku la Lachisanu:

1- Kupereka salaam, monga tiperekera moni mwachilamulo cha Chisilamu, pomwe khatib akuchita khutba.

2– Kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem imam akuchita khutba.

3- Kunena kuti, **"Yarhamukallah,"** kwa munthu amene akuyetsemula kenako ndi kunena kuti, "Al-hamd-u-li-llah," imam akuchita khutba.

---

[1] Chonde onani ndime ya khumi ndi chitatu pa mutu wakuti, 'Adabs za udhu' m'mutu wachiwiri wa gawo lachinayi la **Endless Bliss**, kapena *lowani pa Google ndi kulemba mawu oti 'miswak' kuti muwone momwe Chisilamu chinatiphunzitsira, zaka zopitilira mAdhana khumi ndi anayi zapitazo, momwe tingasamalire mano athu, pakamwa, ndi ngalande zam'mimba***.**

4- Kudya ndi kumwa pa nthawi ya Jummah ndi khutba wake.

5- Kuchita chinthu chomwe chili makruh. [Mchitidwe wa makruh, mwachitsanzo, khatib kutalikitsa nkhani m'dzina la khutba.]

Adhan yoyamba Lachisanu ikayitanidwa, yomwe imachitika pa minaret kunja kwa mzikiti, khatib amaswalin sunnah ya Swalah ya Lachisanu yoyamba pafupi ndi minbar (mwimbali).

Akatha amapita kutsogolo kwa minbar ndi kunena pemphero lalifupi ataima kuyang'ana ku Qibla. Kenako amakwera pa minbar ndi kukhala atatembenukira ku jama'ah ndipo amamvera adhan ya chiwiri. Adhan yachiwiri ikatha, amayimilira ndi kuyamba kupereka khutba.

[Anthu otchedwa Wahhabi sali m'Madhhab a Ahl assunna. Iwo satsatira madhhab ena aliwonse. Amatchedwa ma **Wahhabi** kapena ma **Najdi**. ChiWahhabi chinakhazikitsidwa ndi achiwembu a ku Britain. Iwo anakhazikitsa izi pomugwiritsa ntchito munthu wa chipembedzo wonyozeka ndi mbuli wochokera ku Nejd dzina lake Muhammad mwana wa Abd-ul-wahhab. M'mabuku awo Asilamu omwe sali ma Wahhabi amawatchula kuti ndi makafiri. Mukulemba kwawo akuti ndi kololedwa kupha anthu omwe sali ma Wahhabi ndi kulanda akazi awo, ana awo akazi ndi chuma chawo ngati zolanda pa nkhondo (ghanimat). Mosakaza kwambiri anapereka ziphuphu kwa anthu osazindikira za chipembedzo ndi opanda madhhab ndi kuwagwiritsa ntchito pa za upanduzi, powaphunzitsa chi Wahhabi ndikuwatumiza m'malo otchedwa **Rabita-t-ul 'alam-il-islami.** Malo amenewa anawakhazikitsa m'maiko osiyanasiyana pa dziko lonse lapansi.

Mabuku awo otsutsana ndi Chisilamu omwe amawati ndi 'Ma Fatwa operekedwa ndi mgwirizano wa akadaulo a Chisilamu a padziko lonse,' anafalitsadwa m'maiko onse a Chisilamu. Mu nthawi ya Haji amagawa izi kwaulere kwa hadjis (Asilamu omwe akuchita mapemphero a Hajj). M'chimodzi mwa zolemba zawo akuti: "Ndi fardh kwa akazi kuswali Swala ya Lachisanu." Amakakamiza akazi kukapemphera Lachisanu. Amachita Swalah m'magulu osakanikirana, amuna ndi akazi kuchitira Swalah limodzi pa jama'at. Zikunenedwa m'chimodzi mwa zofalista zawo: "Khutba ya la chisanu ndi Eid ziwerengedwe m'chinenero chomveka kwa Asilamu omwe akuchita jama'at. Isamawerengedwe m'chinenero cha Chiarabu." Akadaulo a chowonadi a Chisilamu m'maiko a Chisilamu amatsutsa fatwa zawo zoterozo popereka umboni wa m'malemba otsimikizira. Zina mwa zotsutsana mabodza amenewa ndi fatwa zoperekedwa ndi akadaulo a Ahl as-Sunnah m'madera osiyanasiyana a India. Mwachitsanzo, Allama

hibr-un-nihrir wa-l-fehhama sahib-ut-taqrir wat-tahrir Mawlana Muhammad Tami bin Muhammad Madrasi 'nawar-Allahu marqadahu', Mufti waku Madras, akunena motere:

Ndi makruh kuchita, kuwerenga, kulakatula kapena kunena khutba m'chinenero chosakhala Chiarabu kapena kuphatikiza Chiarabu pomasulira m'chinenero china. Ndi wajib kuchita khutba yonse mu chiyankhulo cha Chiarabu. Pakuti, Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" adachita khutba zake zonse mu chiyankhulo cha Chiarabu. Zanenedwa m'mutu wokamba za Swalah za Eid m'buku lotchedwa **Bahr-ur-rasiq** kuti:

"Nafila (Swalah zowonjezera, kupatulapo Swalah ya Tarawih ndi Kusuf, sizimachitika pa jama'at. Popeza kuti Swalah za Eid zimachitika nthawi zonse pa jama'at, ziyenera kukhala wajib, osati nafila. Monga taonera, kupembedza kumene Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anachita mosadukiza ndi wajib. Allama Zabidi "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akunena motere mu ndemanga yake pa **Ihya-ul'ulum:** "Mchitidwe wopembedza umene Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam"amachita nthawi zonse ndi wajib. Sikuti zochitikazo zili fardh. Allama Mufti Abu-s-su'ud Efendi "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akunena m'bukhu lake lotchedwa **Fat-h-ullah-il-mu'in**: "Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" atachita izi nthawi zonse osalekeza, zimasonyeza kuti ndi ntchito zopembedza zomwe zili wajib." Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akunena motere mu nkhani yake pofotokoza za Sunnah zosamba kuti: "Mchitidwe wopembedza umene Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ankachita mokhazikika ndi Sunnah-imuakkada ngati sadausiye. Ngati sanachinyalanyaze koma samachita kanthu munthu wina atapanda kuchita, ndiye kuti ndi wajib. Poti kusachita kanthu munthu atachisiya kumakhala kuvomereza kuti chitha kusiyidwa. Pachifukwa chimenecho, Abus-su'ud Efendi ananena kuti, kulambira kumene Mtumiki wodalitsika ankachita mosasiya ndi wajib." Zanenedwa kumapeto kwa gawo lomwe likufotokoza za makruh a Swalah kuti ndi makruh tahrimi kusiya mwa chimodzi.] Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" pochita khutba nthawi zonse mu chinenero cha Chiarabu ndi chizindikiro choti ndi wajib kuchita khutba mu chiyankhulo cha Chiarabu. Choncho, ndi makruh tahrimi kuchita khutba mu chiyankhulo china chilichonse kupatula Chiarabu kapena kuchita m'Chiarabu ndi kutanthauzira. Pakuti pokutanthauzira, lamulo lakuti khutba izichitika m'Chiarabu lidzakhala litaphwanyidwa; ndipo potsirizira pake lamulo loti khutba izichitika m'Chiarabu mokha lidzakhala litaphwanyidwa Muzonsezi, chinthu chomwe Rasulullah

“sallallâhu alaihi wa sallam” ankachichita mosalekeza chidzakhala chitanyalanyazidwa. Momwemonso kunena takbir ya iftitah, (kunena kuti “Allahu akbar,”) m’chiyankhulo cha Chiarabu mukamayamba Swalah ndi kunena kuti “Allahu akbar,” chamkatikati ndi zinthu ziwiri zosiyana. Ndi makruh tahrimi kusiya imodzi mwa izo. Pakuti ndi wajib kutero chifukwa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” nthawi zonse ankati, “Allahu akbar,” Pachifukwa chimenecho, kumakhala makruh tahrimi kusatero. Ibni Abidin “rahima-hullâhu ta’âlâ!” akunena motere mu **Radd-ul-muhtar:** “Makruh ndi mchitidwe kapena khalidwe lomwe mukachita kapena osachita, chunthu chomwe chili wajib kapena Sunnah chimaphwanyika.

Kuphwanya chinthu chomwe chili wajib ndi makruh tahrimi; ndipo kuphwanya Sunnah ndi makruh tanzihi. Zalembedwa motere m’bukhu lotchedwa **Halabi-i-kebir** lolembedwa ndi Ibrahim bin Muhammad Halabi (866, Haleb [Aleppo] – 956 [1549 AD]): “Ndi makruh tanzihi kusiya kapena kuphwanya chinthu chomwe ndi Sunnah. Ndi makruh tahrimi kusiya kapena kuphwanya chinthu chomwe chili wajib.” Zalembedwa m’bukhu lotchedwa **Fatawa-i-Sirajiyya** lolembedwa ndi Ali Ushi bin Uthman “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih” (d. 575 AD. 1185 AD.]) motere “Ndi kololedwa kuchita khutba m’chiyankhulo cha chi Farisi (Persian).”

Zingakhale batil (zopanda pake) kugwiritsa ntchito mawu awa ngati umboni ndi kupereka fatwa yoti ndi kololedwa kuchita khutba mu chiyankhulo china osati Chiarabu ndi kuti kuterosi makruh tahrimi kapena tanzihi. Pakuti mawuwa mu chi Sirajiyya akutanthauza kuti “sahih (chovomerezeka)”, zomwe sizikutanthauza kuti “si makruh.” Ibni Abidin “rahima-hullâhu ta’âlâ!” akunena mu **Radd-ul-muhtar** kuti: "Mukunena kwake, (kwa Ali Ushi's,) kuti sahih sizikusonyeza kuti si makruh." Muhammad Abd-ul-Hayy Luqnevi “rahima-hullâhu ta’âlâ!” akufotokoza m’bukhu lake lotchedwa **Umdet-ur-riaya**: “Mawu akuti ‘kuchita khutba m’chinenero cha Chiarabu si choyenereza kuti Swalah ya Lachisanu ikhale yovomerezeka. Ndi kololedwa kuchita khutba m’Chi Persia kapena m’chinenero china chilichonse.’ Mauwa akusonyeza kuti Swalah yochitika potero ikhala yololedwa. Mmau ena chichititsa kuti Khutba wa Swalah ya lachisanu ikhale yovomerezeka chakwaniritsidwa. Koma sizikusonyeza kuti khutba wochitikawo ndi wopanda karahat (chinachake choupangitsa makruh). Poti Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” ndi ma Sahabah onse “radiyallâhu ’anhum” nthawi zonse komanso kulikonse amachita khutba m’chiyankhulo cha Chiarabu chokha. Ndi makruh tahrimi kuchita

motsutsana nawo.” Komanso ma Tabiin ndi Tabai tabiin1 “rahima-hullâhu ta’âlâ!” ankachita khutba m’chinenero cha Chiarabu, nthawi zonse komanso kulikonse. Sikuti ankachita m’chiyankhulo cha Chiarabu kokha, komanso palibe ngakhale m’modzi mwa iwo amene adachita m’chiyankhulo cha Chiarabu ndikumamasulira m’chinenero china. [Zimenezo ndi zomwe zidalinso m’maiko monga Asia ndi Africa, kumene anthu ankamvetsera khutba asakumvetsa zimene zinkanenedwa mu khutba chifukwa sankadziwa Chiarabu. Ngakhale kuti kunali koyenera kwa iwo kulongosola zonenadwa mu khutba kuti aphunzitse Chisilamu kwa Asilamu atsopano, iwo sanaone kuti nkololedwa kugwiritsa ntchito ziyankhulo zina kusiyapo Chiarabu pa khutba wawo. Amawauza anthu za Chisilamu pa zochitika zina osati kudzera mu khutba.

Iwo amawalangiza kuti aphunzire Chiarabu ndi cholinga choti adzimvetsetsa khutba komanso kuphunzira Chisilamu bwino. Nafenso tiwatsanzire akadaulo amenewa pankhaniyi.]

Ndi **bidah** kuchita mosemphana ndi iwo popereka khutba m’ziyankhulo zina osati Chiarabu. Ndi makruh tahrimi kutero. Ndi batil kuyitcha nkhani yoyambayo 'tahrimi ndi yomaliza 'tanzihi'. Poti makruh tanzihi imatanthauza kusiya chinthu chomwe chili Sunnah. Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” nthawi zonse ankachita khutba m’chinenero cha Chiarabu chokha. Ndi wajib kuchita khutba m’chinenero cha Chiarabu chokha. Zingakhale bwanji tanzihi kusiya kuchita chomwe chili wajib? Ndi wajib kupewa kuchita chinthu chomwe ndi makruh tahrimi. Mawlana Bahr-ul-ulum “rahima-hullâhu ta’âlâ!” akunena motere mu **Erkan-ul-arba’a:** “Ndi wajib kusachita chinthu chomwe chili makruh tahrimi. Kuchita makruh ndiko kuphwanya lamulo (lotchedwa) wajib.”

Munthu amene nthawi zonse amachita makruh tahrimi si Msilamu wa adil. Ibni Abidin “rahima-hullâhu ta’âlâ!” akufotokoza motere kuchokera kwa Ibni Nujaym “rahima-hullâhu ta’âlâ!” pamene akuyamba nkhani yake yokhudza udhu mu bukhu lake lotchedwa **Radd-ul-muhtar** “Ndi tchimo laling'ono kuchita chinthu chomwe ndi makruh tahrimi. Kuchitachita machimo ang'onoang'ono kumamchotsera Msilamu 'adalat (chilungamo) chake. Machimo ang'onoang'ono akabwerezedwa kapena tchimo linalake laling'ono lomwe lachitika kangapo limapanga tchimo lalikulu. Ndipo tchimo lalikulu lomwe lachitika mosabisa limachititsa Msilamu kutaya 'adalat

[1] Mibado yptsatira pambuyo pa Sahabah

yake, kotero kuti sakhalanso Msilamu wa 'adil." Pachifukwa chimenecho, ma khatib omwe amachita khutba muziyankhulo zawo zotanthauzira amataya adalat ndikukhala Asilamu a fasiq. (Zowonadi, Msilamu wa fasiq ndi Msilamu amene amachita limodzi mwa machimo akulu mowonekera. Zitsanzo za machimo akulu ndi: kusachita malamulo limodzi lowonekera m'Chisilamu popanda udhr, kapena kuchita chimodzi mwa zoletsedwa (haram) mosabisa.) Ndi makruh tahrimi kuswali swalah yotsogozedwa ndi anthu oterowo. Zalembedwa m'bukhu lotchedwa **Nurul-idhah**, lolembedwa ndi Abul-Ikhlas Hasan bun Ammar Shernblali "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", 994 - 1069 [1658 AD], Egypt,) komanso mu **Ibni Abidin** motere: "Ndi makruh kwa kapolo kapena munthu wa kumuzi kapena mwana wamamuna obadwa mnjira yosavomerezeka, ngati sanaphunzire, ndi kwa a bid'at, ngakhale ali ophunzira, kukhala imam ndi kutsogolera Swalah ya jama'at. Ndi tchimo kuwasiya iwo kukhala imam ndi kutsogolera Swalah ya Jama'at. Allama Ibrahim Halabi "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akunena mu **Halabi-i-kebir** kuti:

"Asilamu omwe akulola anthu a fasiq kukhala imam ndi kutsogolera Swalah ya jama'at adzakhala akuchita tchimo. Pakuti ndi makruh tahrimi kulola anthu a fasiq kukhala imam." Kwalembedwa mu **Meraq-il-felah** kuti: "Ndi makruh kumulola munthu wa fasiq kukhala imam ndikutsogolera Swalah ya jama'at ngakhale atakhala ophunzira m'Chisilamu. Chifukwa iye ndi wosalabadira potsatira malamulo a Chisilamu. Choncho zili wajib kunyozera za iye. Kumulola kukhala imam kumatanthauza kumulemekeza. Ngati simungate kumuletsa kutsogolera Swalah ya Jama'at, ndiye kuti muzikaswali Swalah ya la chisanu ndi Swalah zina zonse za Jama'at mu msikiti wina. Monga momwe Allama Tahtawi "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akulongosora ndime iyi motere: "Ndi makruh tahrimi kwa Asilamu kulola munthu wa fasiq kukhala imam potsogolera Swalah yawo ya jama'at."

Musamuchititse khatib kupereka khutba m'chinenero china chosakhala Chiarabu. Ndi tchimo kuyambitsa izi. Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ!" akunena mu **Radd-ul-muhtar**: "Swalah ya jama'at siyiyenera kutsogoleredwa ndi imam wa fasiq. Muyenera kuyang'ana imam yemwe Sali wa fasiq. Swalah ya la chisanu ndi nkhani yosiyana.

Komabe, ngakhale Swalah ya la chisanu ndi makruh kutsogoleredwa ndi imam wa fasiq ngati kuli misikiti ina komwe swalah ya Jumu'ah ikuchitika. Poti muli ndi ufulu wotsogoleredwa ndi imam wina mu msikiti wina. Bukhu lomwe mutu wake ndi **Fat-h-**

ulqadir[1] limakamba nkhani yomweyo." Choncho, musaswali pambuyo pa imam yemwe akuchita khutba m'chiyankhulo chachiwiri chomwe akumasulira m'malo mochita m'Chiarabu mokha, ndipo fufuzani imam amene amachita khutba m'Chiarabu ndi kuswali Swalah ya Jumu'ah pa mbuyo pa imam ameneyo. Kuti mudziwe zambiri, werengani bukhu lotchedwa **Et-tahqiqat-us-saniyya fi-karahat-il-khutba-ti-bi-ghayri-l-'arabiyya wa qiraatiha bi-l'arabiyyat-i-ma'a terjemetiha bi-ghayr-il-'arabiyyati.** Apa tikumaliza kumasulira kwathu kuchokera ku zolemba za Allama Muhammad Temimi Madrasi.

Zolemba zili pamwambazi, zomwe zinalembedwa m'Chiarabu ku India mu 1349 [1931 A.D.], zinavomerezedwa ndi kusayinidwa ndi akadaulo khumi ndi atatu ozindikira kwambiri za Chisilamu ku India. Limodzi ndi fatwa imeneyi yomwe ili ndi mbiri yodziwika bwino, ma fatwa, a Chiarabu a akadaulo aku India ochokera ku **Diobend, Baqiyat-us-Saalihat, Madras** ndi **Haydarabad** anasindikizidwa ku Istanbul, Turkey, mu 1396 [1976 A.D.].

Zikwizikwi za Asilamu ophunzira mozama ndi ma sheikh a Chisilamu odziwika bwino a nthawi ya Ottoman "rahima-hullâhu ta'âlâ!" anafufuza njira zothandizira kuti anthu amvetse khutba yomwe ankamvetsera. Polephera kupeza umboni owaloleza kuwonjezera kutanthauzira Khutba mu Chituruki, iwo sanapereke chilolezo kuti zingatero. Cholinga chowaunikira Asilamu omwe amachita Jama'at chidakwaniritsika pokhazikitsa ulaliki wa la chisanu m'misikiti yonse pa kutha pa Swalah ya la chisanu, Anthu m'misikiti anayamba kudziwitsidwa zomwe zinali m'ma fatwa kwa zaka mazana asanu ndi limodzi (600), ndipo potero machitidwe a Chisilamu adatetezedwa kuti asapwanyidwe.]

Swalah ya Eid ili ndi ma Takbir asanu ndi anayi (9) omwe amatchedwa **Takbir Zawaid**: Imodzi mwa iwo ndi fardh. Ina ndi Sunnah. Asanu ndi awiri (7) mwa iwo ndi wajib. Takbir iftitah ndi fardh. Takbir ya Ruku yoyamba ndi Sunnah. Ma takbir a zawaid ndi wajib. Takbir ya Ruku mu raka'at yachiwiri ndi wajib chifukwa chogwirizana ndi takbir ina yomwe ndi wajib; komanso ndi yomaliza mwa ma takbir asanu ndi awiri a zawaid, nayonso ndi wajib).

[1] Linalembedwa ndi Ibni Humam "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (730 [1388 AD] - 861 [1456]) monga ndemanga ya buku la Hidaya, lomwe linalembedwa ndi Burhanaddin Merghinani "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih"(593 [1197 AD] - anaphedwa ndi magulu a Jenghiz Khan.)

KUYIMIKA SWALAH

Zinalembedwa motere mu **Ni'mat-i-islam**: Ndi fardh kwa Msilamu aliyense wozindikira komanso wokhwima kuswali kasanu pa tsiku. Palibe yemwe angachite Swalah m'malo mwa munthu wina. Munthu akhoza kupereka thawab ya Swalah kapena ntchito ina ya kupembedza yomwe angachite kwa munthu wina, wamoyo kapena wakufa. Wopatsidwa thawabyo adzalandira thawab mofanana ndi zomwe wapeza woperekayo, ndipo palibe thawab yomwe idzapungulidwe kwa woperekayo.] Sikololedwa kuchita Swalah ndikupereka thawab zomwe wapeza kwa wamangawa wako kapena wangongole ndi cholinga choti akukhululukire za ma ufulu awo omwe aphwanyidwa. Munthu yemwe amakhulupilira kuti swalah zisanu pa tsiku ndi fardh koma osaswali popanda udhr, sangakhale kafiri. Iye adzakhala Msilamu wa Fasiq. [Kwanenedwa m'mabuku odalirika a Chisilamu kuti chilango cha kuphonya Swalah imodzi ndi Jahannam kwa zaka 70,000.] Munthu amene sakuswali kasanu pa tsiku adzatumizidwa kundende ndipo adzasungidwa kumeneko mpaka atayambanso kuswali.

Mwana akakwanitsa zaka zisanu ndi ziwiri (7) adzalamulidwa ndi makolo ake kuswali. Ngati sakuswali pa msinkhu wa zaka khumi, amenyedwa ndi manja. Asamenyedwe mbama zopitilira zitatu. Asamenyedwenso ndi ndodo. Kumenya ndi ndodo ndi chilango choyenera munthu wachikulire yemwe wapalamula mulandu wakupha, ndipo pakufunika chigamulo cha khoti. Mamuna sangamenye mkazi wake ndi ndodo [Sizololedwa kumenya cha moyo chilichonse pa mutu kapena kumaso kapena pachifuwa kapena kutsogolo kapena pamimba.] Ndi fardh'nso kwa amene alibe kuthekera kuti achite Swalah momwe angakwanilitsire ndi mphamvu zawo.

KUKHALA NDI UDHR

Ngati china chake chikutuluka kuchokera m'thupi la munthu mosalekeza, chimatchedwa 'udhr', ndipo munthu amene akukumana ndi vuto loteleri timati ali 'udhr'.) Munthu amene akuvutika ndi kugula kwa mmimba, kusadziletsa kwa mpweya, kutuluka magazi m'mphuno kapena pachilonda, mafinya ochokera pa chilonda kapena zilonda za mmimba, misozi yotuluka chifukwa cha kutupa kapena zilonda za mmaso ndi zina zotero, amatchedwa **anthu omwe ali ndi 'udhr.** Mkazi yemwe akudwala **istihada** (nsambo osalekeza) naye ali gulu lomweli.

Anthu awa ayenera kuthetsa chimene chikuyambitsa ‘udhr’ pogwiritsa ntchito njira monga kutsekapo, mankhwala, ndi kuchita Swalah atakhala kapena pochita zizindikiro [Mamuna yemwe ali ndi vuto la mkodzo wosalekeza, alowetse thonje longochokera mmunda lalikulu ngati njere ya bale mu ngalande yake ya chokodzera. Kugwiritsa ntchito thonje lopangidwa kumaopsya kuti mwina ulusi wake ukhoza kulowa mu impso ndi kuyambitsa matenda. Pokodza, thonjelo limatuluka lokha. Ngati mkodzo ukuchulukirachulukira mchikhodzodzo, wosefukira umadutsa mu thonje ndi kutuluka, zomwe zimachititsa kuti udhu wa munthuyo uwonongeke. Mkodzo womwe ukutuluka usawononge kabudula wamkati, zomwe zingapewedwe pokulunga nsalu pa chiwalo chokodzera ndipo zikhoza kupangidwa mofulumira ndi ulusi wosokedwa pangodya ya nsaluyo ndi kumangilira ku kabudula wamkati motetezedwa ndi pini. Ngati mkodzo ukutuluka wochulukabe, thonje lina likhoza kuyikidwa munsalu. Ngati komasula kumapeto kwa ulusi kuli kovuta kuchoka ku pini yotetezera, pini wopanila mapepala akhoza kuyikidwa ku pini yotetezerayo ndipo chomasuliracho chikhoza kupachikidwa pa pini wa mapepalayo. Zidzakhala zosavuta kumasulira kuti nsaluyo ichapidwe katatu mu beseni. Munthu amene ali ndi vuto la mkodzo ayenera kunyamula nsalu zitatu kapena zisanu m’thumba mwake. Kukonza kachidutswa ka nsalu ndi ulusi, ngodya imodzi ya nsalu yokwana 12x15 cm imapotedwa ndipo chingwe chopota chotalika 50 cm. chimangidwa pa ngodya yopotayo.

Kwa anthu okalamba ndi ena ofooka, chokodzera chimafota, kotero kuti nsalu yotchinga imakanika kumanga. Anthu oterowo amayika nsalu yayikulu ngati mpango m'thumba laling'ono ndipo amayika chokodzera ndi mipila yomwe m'kathumbako. Ndipo amamanga kukamwa kwa kathumbako. Ngati kuchuluka kwa mkodzo pansalu kukupitilira dirham imodzi (4.80 gr.), nsaluyo iyenera kusinthidwa. Nthawi ya Swala ikatha, udhu wa munthu yemwe ali ndi ‘udhr umatha. Ngati powonjezera pa ‘udhr womwe ulipo kale, chifukwa china cha udhr chikaoneka nthawi ya swala isanathe, udhu wawo umakhala opanda pake chifukwa cha udhr yatsopanoyo yomwe yapezeka nthawi ya swala isanathe. Mwachitsanzo, yerekezani kuti mwatsuka pomwe pakutuluka magazi (mosalekeza) kuchokera m'mphuno yanu imodzi; kutsuka uku kumakhala kopanda phindu ngati magazi ena ayamba kutuluka kuchokera mu mphuno yanu ina. M’Madhhab a Hanafi ndi a Shafi’i, kukhala munthu wa ‘udhr’ ndiye kuti uli ndi vuto losalekeza lomwe limaononga udhu nthawi ya

mapemphero. Mwachitsanzo, ngati magazi a munthu asiya kwa nthawi yochepa moti sayambiranso mpaka munthuyo kumaliza kupanga udhu ndikuchita gawo la fardh la Swalah ya nthawi ya Swala, ndiye kuti munthuyo alibe ‘udhr. Munthu akakhala kuti ali ndi ‘udhr, kukhala kwake kumapitilira mu nthawi zonse za mpaka Swalah yotsatira malinga ngati zomwe zimayambitsa udhr wake zimabwerezedwa nthawi iliyonse mwa nthawi zimenezo. Teyerekeze kuti magazi akutuluka kamodzi kokha mkati mwa nthawi iliyonse swalah, kaya dontho limodzi la magazi lomwe limawoneka. Ngati magazi satulukanso mkati mwa nthawi yopemphera, munthuyo sakhalanso ndi 'udhr. Ngati Najasi yoposa dirhamu imodzi ndi yomwe yayambitsa ‘udhr popaka zovala za munthuyo, n’koyenera kutsuka gawo lomwe lapaka Najasi ngati kuli kotheka kupewa kudzipakanso.

Zafotokozedwa motere m'bukhu la **al-Fiqh-u-'ala-l-Madhahib-il-erba'a**: "Pali ma qawl awiri onena za munthu yemwe alibe kuthekera kuti ali ndi 'udhr molingana ndi Madhhab a Maliki: Malinga ndi qawl yoyamba, chinthu chomwe chikuononga udhu chiyenera kupitilira theka la nthawi ya Swalah ndipo chikhala choti sichikudziwika kuti chinayamba liti ndipo chinatha liti. Malinga ndi qawl yachiwiri, wodwala amakhala munthu 'udhr pamene kosapeweka kumayamba mopanda kupezeka kwa mfundo ziwiri za mu qawl yoyamba.

Udhu wa muthu yemwe alibe kuthekera siumawononge ka. Ngati nthawi yomwe kutuluka kwa madziko kwadziwika, zili mustahab kwa wodwalayo kuchita udhu asanayambe kuswali. Munthu wodwala kapena wokalamba amene amatsatira Madhhab a Hanafi ndi Shafi’i ndipo sali munthu wokhala ndi ‘udhr (malinga ndi Madhhab awiriwo) atsate qawl ya chiwiri ya Madhhab a Maliki.”]

Ngati munthu akuwopa kuti angadwale, kapena kuti matenda ake angakule kapena kuchedwerapo kuchira ngati atachita udhu, ndiye kuti achita tayammamu. Manthawa akhala otengera zomwe munthuyo anakumana nazo kapena malangizo a dokotala wa Msilamu yemwe ndi adil. Uphungu wa dokotala ndi wovomerezeka malinga ngati sali ochita za utchimo. Zina zomwe zingayambitse matenda ndi izi: Kuzizira komanso kusakhala ndi pogona; kulephera kupeza chotenthetsera madzi kapena ndalama zolipilira kosambira. M’Madhhab a Hanafi mutha kuswala Swalah za fardh zambiri momwe mungafunire ndi tayammam imodzi yomwe mwapanga. M’Madhhab a Shafi’i ndi Maliki muyenera kuchita tayammam yatsopano pa Swalah ya fardh iliyonse.

Ngati munthu ali ndi zilonda pa theka la ziwalo zake zoyenera kuthira madzi pochita udhu, iye achite tayammamu m'malo mothira madzi. Ngati zilondazo zili zosakwana theka la ziwalo zofunika kuthira madzi, ndiye kuti munthuyo athire madzi mbali zomwe zili bwino ndi kuchita masah pachilondapo. Popeza thupi lonse limatengedwa ngati chiwalo chimodzi mu ghusl, ngati theka la thupi lanu lili ndi zilonda zowawa zotuluka mafinya, mumachita tayammam. Ngati gawo lomwe lili ndi zilonda zotuluka mafinya ndi lochepera theka la thupi lanu lonse, ndiye kuti mumatsuka gawo labwinolo ndi kuchita masah pachilonda. Ngati kuchita masah pachilonda kungawonjezere ululu wa zilondazo, ndiye kuti mumachita masah pa bandeji.

Ngati kutero nakonso kudzakhala kowawa, ndiye kuti musachitenso masah. Ngati, pochita udhu kapena ghusl, masah pa mutu panu zili zowawa, ndiye kuti simuchita masah pa mutu panu. Munthu amene sangathe kugwiritsa ntchito madzi ndi dzanja lake chifukwa cha chinthu china chovuta ndi madziwo monga chipere kapena zilonda zotuluka madzi, iye ayenera kuchita tayammam. Pochita tayammam, amapukuta nkhope ndi manja mofatsa pa dothi kapena pa khoma lopakidwa ndi laimu kapena pa mwala. Tiyerekeze kuti munthu alibe manja ndi mapazi komanso ali ndi zilonda kumaso kwake, ndiye kuti amachita Swalah osachita udhu. Munthu amene sangapeze womuthandiza kuchita udhu amachita tayammam. Ana ake, akapolo ake kapena a ntchito ake amuthandize kuchita udhu. Atanso kupempha ena kuti amuthandize. Koma ena sakufunikira kuti amuthandize. Mamuna ndi mkazi sayenera kuthandizana wina ndi mnzake kuchita udhu.

Tiyerekeze kuti munthu akugwiritsa ntchito bandeji kapena pulasitala yemwe wakulungidwa pa nsalu yopyapyala kapena thonje ndi mafuta pofuna kuletsa kutchutcha kwa magazi kapena mphusi zoyamwa magazi kapena chilonda chotuluka magazi kapena chotupa kapena fupa lothyoka kapena lovulala; ngati sangathe kusambitsa malo amenewa ndi madzi ozizira kapena otentha ngakhale kuchitapo masah, ndiye, pomwe akuchita udhu kapena akusamba, adzangochitapo masah kopitilira theka la malowo kamodzi. Ngati kungakhale kovuta kumasula bandeji, malo apansi pake sayenera kuwasambitsa. Masah imachitika pa malo a khungu omwe ali bwino owonekera mu bandeji. Ndikofunikira kukhala ndi udhu pa nthawi yomwe mukukulunga bandeji. Ngati bandejiyo yasinthidwa mutachita masah, masah pa bandeji yatsopanoyo ndi yosafunikira, ngakhale atamangidwa ina.

SWALAH NTHAWI YA MATENDA

Zinalembedwa motere mu **Ni'mat-i-islam**:

Ngati munthu wodwala satha kuyima kapena akukhulupirira kwambiri kuti kuyimilira kudzakulitsa matenda ake, ndiye kuti amachita Swalah atakhala; amapinda tupi lake pang'ono pochita Ruku; ndipo kenako kukhala. Amachita sajda pogunditsa mphuno ndi chipumi pansi. Ndipo amakhala mmene akumverako bwino. Ndi zololedwa kwa iwo kugwada kapena kukhala mopingasa miyendo kapena kugwada ndi matako awo ndi manja awo mozungulira mawondo awo atawakokera pafupi ndi matupi awo. Kupweteka kwa mutu, dzino ndi zilonda zamaso zimatengedwa kuti ndi matenda. 'Udhr ina pankhaniyi ndi mantha kuwopa kuwonedwa ndi mdani. Komanso, munthu amene udhu wake ugaonongeke chifukwa choyima amachita Swalah atakhala. Munthu amene angayime potsamira chinachake amachita Swalah atatsamira. Munthu wolephera kuyima kwa nthawi yayitali amachita takbir ya iftitah, ponena, "Allahu akbar," atayima, ndikupitiriza Swalah yake ndikukhala pomwe wamva kuwawa.

Munthu amene sangathe kuchita sajda pansi amawerenga ma ayah ali chiyimire kenako nndi kukhala pansi kuchita Ruku ndi sajda ndi zizibdikiro. Izi amachita popinda matupi awo pang'ono pa Ruku ndi kuzipinda mowonjezera pa sajda. Anthu omwe amalephera kupinda matupi awo amapinda mutu. Nkosafunika kwa anthu otere kuchita sajda pa chinthu. Ngati achita sajda pa chinthu, Swalah yawo idzakhala Sahih ngati kuzipinda kwawo pa sajda kwawonjezereka kuposa kuzipinda kwawo pa ruku. Koma adzakhala atachita makruh poti ndi makruh kuchita sajda pa chinthu chomwe chimachititsa malo a sajda kukhala okwera kuposa mulingo. Ndi kosaloledwa kugona ndi kuchita Swalah ndi zisonyezo ngati kuli kotheka kukhala ndi kutsamira (pa chinthu).

Mtumiki wathu wodalitsika "sallallâhu alaihi wa sallam" anaona odwala akuchita sajda pa pilo yomwe anayika patsogolo pake; Iye anatenga piloyo ndikutaya. Pamenepo munthuyo anayika chinthu cha thabwa patsogolo pake. Wopambana mzolengedwa zonse anatayanso, nati: "**Chitira pa nthaka,** [komwe ndikuyika chipumi chanu pansi,]! **Ngati simungathe kutero, chitani zizindikiro, pindani (thupi lanu) kwambiriko pa sajda kusiyana ndi momwe mupindire pa Ruku!"** Monga zanenedwera m'bukhu lotchedwa **Bahr-urraiq** lolembedwa ndi Zaynal'abidin bin Ibrahim ibni Nujaym-i-Misri "rahmatullâhi

ta'âlâ 'alaih", 926 - 970 [1562 AD] wa ku Egypt, ngati ndemanga ya bukhu lotchedwa **Kenz-ud-daqaiq**, lomwe linalembedwa ndi Abul-barakat Hafidh-ud-din Abdullah bin Ahmad Nasafi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", 710 [1310 AD] wa ku Baghdad, kuti zikunenedwa mu ayati karima 191, Surah Al Imran "Amene angathe kuswali atayima, aswali atayima. Amene sangathe kutero aswali atakhala. Ndipo ngati sangathe kukhala, aswali atagona." Pamene Imran bin Husayn "radiyallâhu anh" anadwala, Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam"adati kwa iye: **"Chita** (Swalah) **uli chiyimire! Ngati siungathe kutero, chita utagona chammbali kapena chakumbuyo."** [Monga taonera, wodwala amene sangayime aswali atakhala. Amene akukanika kukhala pansi aswali atagona. Ndizosaloledwa kwa munthu amene akutha kukhala pansi kapena kwa amene ali paulendo wa pa basi kapena pa ndege kuchita Swalah atakhala pa mpando ndi mapazi ake ali neng'a. Ngati munthu sangathe kuchita Swalah pa jama'at atayima mu mzikiti, aswali atayima ku nyumba kwake. Pali udhr makumi awiri (20) zolola kuti munthu asapite ku mzikiti kukaswali mu jama'at. Zinthu zotsatirazi ndi 'udhr zomwe zingalepheretse kuchoka kumalo anu okhala kukapemphera Swalah ya tsiku la chisanu: Mvula; kutentha kwambiri kapena kuzizira kwambiri; kuwopa mdani amene angakupheni kapena kukulandani katundu wanu; kuopa anzanu kukusiyani nokha pa ulendo wanu; mdima wandiweyani; munthu wosauka yemwe ali ndi ngongole kuopa kumangidwa ndi kutsekeredwa m'ndende; kukhala wa khungu; kukhala wopuwala ziwalo kwambiri moti sungayende; kukhala ndi phazi limodzi chifukwa choti phazi lina analidula; kukhala wolumala; matope kwambiri; kulephera kuyenda; kukalamba kwambiri kosatha nako kuyenda; kuwopa kuphonya kalasi yosowa ya Fiqh; kuwopa kuphonya chakudya chimene munthu amachikonda; Kukhala pafupi kunyamuka ulendo; kukhala dokotala wophunzira bwino yemwe alibe womulandira ntchito; usiku wamphepo ya nkhuntho; kupanikizika ndi nkodzo (kapena chimbudzi); kukhala wolumala amene akuwopa kuti matendawo afika poyipitsitsa kapena angachedwe kuchira kapena namwino yemwe akuwopa kuti akachoka pasowa oyang'anira munthu wodwala; kuvutika kuyenda ndi ukalamba. Kuyenda wapansi popita ndi pobwelera ku mzikiti kukapemphera la chisanu ndikwabwino kuposa kugwiritsa ntchito galimoto.

Nkosaloledwa kuchita Swalah ndi zizindikiro mutakhala pampando kapena pasofa mu mzikiti. Ndi **bidah** kuchita zopembedza m'njira yosavomerezeka ndi Chisilamu. Ndipo kwalembedwa m'mabuku a Fiqh kuti ndi utchimo waukulu kuchita chinthu chomwe chili bidah.]

Munthu amene wadwalika moti sangathe kuswali atatembenukira ku Qibla, ayesetse kuchita Swalah potembenukira mbali ina iliyonse yotheka. Ngati wodwalayo wagona chagada chinthu (chofewa) chiyikidwe pansi pa mutu wake kuti nkhope yake ikhale yolunjika ku Qibla. Ndibwino kuyimika mawondo. Ngati munthuyo wadwala kosatha kuchita zizindikiro ndi mutu wake, ndi kololedwa kwa iye kusiya Swalah ndikudzachita qada. Munthu amene wayamba kudwala ali pa Swalah ayenera kupitiriza ndi swala yake mpaka momwe angakwaniritsire. Ngati munthu wodwala yemwe akuswali atakhala akuchira ali pa swalah, apitilize swalahyo atayima. Munthu yemwe mutu wake siukugwira bwino sayenera kuchita Swalah. Wodwala yemwe waphonya Swalah akachira nthawi ya Swalah za pa tsiku isanathe, ayenera kuchita qada ya swalah zonse zisanu kapena zomwe anaphonyazo. Ngati Swala zisanu ndi imodzi zadutsa, samachita qada.

Ndi fardh kuchita qada ya Swalah yomwe mwaphonya kuswali mu nthawi yake machangu, ngakhale pogwiritsa ntchito zizindikiro. Ngati munthu ali pafupi kufa asanapeze mpata woswali qada, sikudzakhala wajib kwa iye kulamula mu wasiyya wake kuti ndalama zokwana fid'ya zilipiridwe kuchokera ku chuma chimene wasiya kulipira Swalah zomwe sanachite. Koma zimakhala wajib kwa iye kutero atachira ndikukhalabe wathanzi ndikupanga qada. Ngati sanalamula mu wasiyya wake, zikuloledwa, malinga ndi kunena kwa akadaulo, kuti Wali wake, kapena munthu wina achite isqat pogwiritsa ntchito chuma chawo. Apa tikumaliza ndime yomwe tinabwereka kuchokera mu **Ni'met-i-islam.**

Zanenedwa motere mu Hadith sharif: **Pali zochita makumi awiri ndi zinayi (24) zomwe zimabweretsa umphawi pa munthu:**

1- Kukodza chiyimire popanda darurat yopangira choncho. (darurat ndi zomwe siungasinthe zomwe zimakukakamiza kuchita kapena kusachita chinachake.)

2- Kudya chakudya uli ndi janaba, (pomwe muyenera kusamba).

3- kunyozetsa zinyenyeswa za bread ndi kuponda

4- Kuwotcha makoko a anyezi ndi adyo.

5- Kuyenda patsogolo pa akuluakulu.

6- Kuyitana kholo lanu potchula zina lawo.

7- Kuthokosa m'mano ndi nthambi za mitengo kapena masache.

8- Kusamba m'manja ndi matope.

9- Kukhala pa chiundo (pa khomo).

10- Kuchitira udhu pa malo pomwe munthu wakodzerapo.

11- Kuyika chakudya m'mapoto ndi kapena mu sefuliya zosatsuka.

12- Kusoka zovala ziri pathupi.

13- Kudya anyezi uli ndi njala.

14- Kuwumitsa nkhope ndi chovala.

15- Kulola akangaude kukhala mnyumba mwanu.

16- Kutuluka mu mzikiti mwachangu mutatha kupemphera Swala ya m'mawa pa jama'at.

17- Kulawilira kupita kumsika ndi kubwerako mochedwa.

18- Kugula mkate kwa munthu wosauka.

19- Kutembelera makolo anu.

20- Kugona maliseche.

21- Kusiya miphika ndi ziwiya zosavundikira.

22- Kuwuzira pozimitsa kuwala monga kandulo.

23- Kuchita chilichonse popanda kunena kuti, "Bismillah."

24- Kuvala buluku lako chiyimire.

Ngati munthu angawerenge Surah "**Inna a'tayna...,"** asanagone kenako ndi kunena kuti, "Ya Rabbi (Oh Mbuye wanga)! Chonde ndidzutseni pa nthawi ya swalah ya m'mawa mawa," Bi-iznillâhi ta'âlâ, munthu ameneyo adzadzuka pa nthawi yake ya swalad ya m'mawa.

KUFUNIKIRA KWA SWALAH

Bukhu lotchedwa **Ashi'at-ul-lama'at** linalembedwa ndi **Abd-ul Haqq bin Seyf-ud-din Dahlawi** "rahima-hullâhu ta'âlâ!", 958 [1551 AD] - 1052 [1642] wa ku Delhi, lili ndi ma Hadithi sharif osiyanasiyana onena za kufunikira kwa Swalah.

Bukhuli ndi ndemanga yolembedwa mu chiyankhulo cha chi Persia ya bukhu la Hadith lotchedwa **Mishkat-ul-Mesabih** lomwe linalembedwa ndi Waliyy-ud-din Khatib-i-Tebrizi Muhammad bin Abdullah "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", d. 749 [1348 AD] ngati ndemanga ndi zowonjezera ku bukhu lotchedwa **Mesabih**) lolembedwa ndi Imam Baghawi Huseyn bin Mas'ud Muhy-is-sunna "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", d. 516 [1122 AD]). **Ashi'at-ul-leme'at** ndi bukhu la magawo anayi. Linasindikizidwa mu 1384 [1964 AD] ku Lucknow, India.

Swalah imatchedwa **'salat'** m'chinenero cha Chiarabu. Tanthauzo loyamba la 'salat' ndi mapemphero, rahmat (Chifundo, Chisoni) ndi istighfar (kupempha chikhululuko cha Allahu ta'âlâ). Poti Swalah ili ndi matanthauzo onse atatu, Swalah imatchedwa 'salat'.

1- Abu Hurayra "radiyallâhu 'anh" anagwira mawu a "sallallâhu alaihi wa sallam" kuti:

"Swalah zisanu za pa tsiku ndi Swalah ya Jumu'ah ndi zimamuwombola munthu ku machismo omwe angachitike mpaka Lachisanu litsatilalo; Ndipo kusala kapena kufunga (kwa masiku makumi atatu) **mu Ramadan ndi kumamuwombola munthu ku machimo omwe angachitike mpaka Ramadhan yotsatirayo. Asilamu omwe amapewa machimo akuluakulu amakhululukidwe ku machimo ang'onoang'ono."** Ntchito izi zimafafaniza machimo ang'onoang'ono omwe akuchitika pa nthawi ino koma omwe sakhudza ufulu wa umunthu. Kwa Asilamu omwe machimo awo onse akhululukidwa, ndipo palibe tchimo lotsala, Swalah ya al chisanu ndi kusala mu Ramadan) zimachepetsa chilango cha machimo awo akulu. Kukhululukidwa machimo akuluakulu kumafunanso kuwachitira tawba. Tawba ndi kulapa machimo omwe wachita, ndi kumupempha Allahu ta'âlâ chikhululuko, kutsimikiza mu mtima kusadzachitanso zoyipazo, ndi kumulonjeza Allahu ta'âlâ kuti siudzachitanso zimenezo. Ngati Msilamu sadachite machimo akulu, ndiye salat ndi Ramadan zimamukweza msilamuyo pa uzimu. Hadithi sharif iyi yalembedwa m'bukhu lotchedwa **Sahih Muslim**. Mapemphero a la chisanu amabweretsa chikhululuko kwa Asilamu omwe Swalah zawo zisanu za pa tsiku zili zowonongeka. Ngati Swalah zawo za Jumu'ah zilinso ndi vuto, ndiye kuti kusala kwawo mu Ramadan kumawachititsa kuti akhululukidwe.

2- Abu Hurayra "radiyallâhu 'anh", akunenanso kuti: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" adati: **"Tiyerekeze kuti pa khomo la nyumba ya munthu pali mtsinje womwe ukuyenda madzi ndipo amasamba kasanu patsiku mu m'mtsinjemo. Kodi padzatsala litsiro pa thupi lake?** "Ayi, sadzatsala ndi litsiro, Iwe Mtumiki wodalitsika wa Allahu ta'âlâ," anayankha ma Sahabah. Pamenepo Rasulullah adati: **"Momwemo ndi momwe ziliri ndi Swalah zisanu za tsiku ndi tsiku. Allahu ta'âlâ amakhululuka machimo ang'onoang'ono a Asilamu omwe amachita Swalah kasanu pa tsiku."** Hadithi sharif iyi yalembedwa mu **Sahih Bukhari** komanso mu **Sahih Muslim.**

3- Abdullah ibni Mas'ud "radiyallâhu anh"akuti: Wina anamupsopsona mkazi amene anali na-mahram kwa iye.

Tsatanetsatane wa nkhaniyi ili motere: Mmodzi mwa ma Ansar amagulitsa zipatso za tende. Mkazi wina anabwera kudzagula tende. Iye anakopeka kwambiri ndi chithupi cha mkaziyo. “Ndili ndi tende wina wabwino kunyumba. Tiyeni ndikakupatseni tende wabwinoko,” adatero. Atapita kunyumba kwake iye anamukumbatira mkazi uja ndi kumupsopsona. "Mukutani? Opani Allahu ta’âlâ,” anadzudzula mkaziyo. Iye analapa. Ndipo anadza kwa Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam” namuuza zomwe anachita. Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”sanamuyankhe, ndipo anadikira wahy1 kuchokera kwa Allahu ta’âlâ. Pambuyo pake munthuyo anachita Swalah. Allahu ta’âlâ adatumiza ayah 114, Surah Hud (kwa Mtumiki Wake wodalitsika). Ayah-karima ikunena kuti: **"Ndipo chitani Swalah nthawi zonse ku mbali ziwiri za tsiku ndi pomwe usiku ukudza! Pakuti zabwino zimachotsa zoipa; ...”** Mbali ziwiri za tsiku ndi dzuwa lisanafike pa liwombo ndi litadutsa pa liwombo. Tsono, Swalah zomwe akutanthauza apa ndi Swalah ya m’mawa (fajr), Swalah yoyamba yamasana (dhuhr) ndi Swalah yachiwiri yam asana (Asr). Ndipo Swalah za kuyandikira kwa usiku ndi Swalah ya madzulo (Maghrib) ndi Swalah ya usiku (Isha). ayati karima iyi ikulengeza kuti mapemphero asanu pa tsiku amabweretsa chikhululuko cha machimo. Munthu wodalitsika anafunsa: “Ya Rasulullahu (Oh Mtumiki wa Allahu ta’âlâ)! Ndi nkhani yabwino kwa ine ndekha?” "**Ndi ya Ummat wanga wonse (Asilamu),"** adatero Mtumiki wodalitsika. Hadith sharif iyi yalembedwa m'mabuku onse awiri otchedwa **'Sahih',** (Sahih Bukhari ndi Sahih Muslim.)

4- Anass bin Malik “radiyallâhu anh” akufotokoza: Wina anadza kwa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” nati: "Ndachita tchimo loyenera chilango cha hadd. Ndikwapulidwe pokwaniritsa hadd.” Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam” sanamfunse kuti walakwa chiyani. Itafika nthawi ya Swalah tinaswali limodzi. Pamene Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anamaliza Swalah, munthu wodalitsikayo anaimilira nati: “Ya Rasulullahu “sallallâhu alaihi wa sallam”! Ine ndachita tchimo kuti ndilangidwe ndi chilango cha hadd. Ndipatseni chilango chomwe chalamulidwa ndi Bukhu la Allahu ta’âlâ! **“Kodi simunaswali ndi ife,”** anafunsa Mtumiki. Munthuyo anati: “Inde, ndatero.” **“Usakhale odandaula. Allahu ta’âlâ wakukhululukira tchimo lako,”** inadza nkhani yabwinoyi kuchokera kwa wokondedwa wa Allahu ta’âlâ. Hadith sharif iyi ili m'mabuku awiri amaziko a Hadith.

[1] *Wahy-chivumbulotso*

Munthu wodala uja anakhulupilira kuti anachita tchimo lalikulu limene anayenera kulangidwa ndi hadd.

Kukhululukidwa chifukwa choti anachita Swalah kukusonyeza kuti linali tchimo laling'ono. Kapena, ponena kuti, "hadd," amatanthauza 'ta'zir', yomwe imaperekedwa ngati chilango cha machimo ang'onoang'ono. Zimenezi ziyenera kuti zinali choncho, popeza sananene kuti, "Muchite hadd pa ine," mukufunsidwa kwake kwachiŵiri.

5– Abdullah ibni Masud "radiyallâhu 'anh" akufotokoza kuti: Ndinamufunsa Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" kuti ndi ntchito iti yomwe Allahu ta'âlâ amayikonda kwambiri**. "Swalah yochita mu nthaŵi yake,"** Anayankha wokondedwa kwambiri mwa olengedwa. Ndipo zanenedwa mu Hadith sharif kuti Allahu ta'âlâ **"amakonda kwambiri Swalah yomwe imachitika m'nthawi yake yoyambilira."** Ndidafunsa kuti ndi ntchito iti yachiwiri yomwe Allahu ta'âlâ amayikonda kwambiri. **"Kukhala wabwino ndi makolo,"** adatero. Ndidafunsa kuti ndi ntchito iti yomwe amayikonda yachitatu, ndipo wodalitsika wa Allahu ta'âlâ adayankha: **"Kuchita Jihad mu njira ya Allahu ta'âlâ."** Hadith sharif iyi yalembedwanso m'mabuku awiri a Sahih. Kwanenedwanso mu Hadithi sharif ina: "**Ntchito yabwino kwambiri ndi kupereka chakudya cha madzulo."**

Mu nkhani inanso: **"Ntchito yabwino kwambiri ndi kufalitsa malonje a Asilamu."** Mu nkhani inanso: **"Ntchito yabwino kwambiri ndiyo kuchita Swalah pakati pa usiku, pamene anthu onse ali mtulo".** Mu Hadith sharif ina: **"Ntchito yofunika kwambiri ndi kuchita zinthu zoti ena asamve kuwawa chifukwa cha manja anu,** (kutanthauza khalidwe) **ndi lilime lanu,** (kutanthauza mawu)**."** Mu Hadith sharif ina: **"Jihad ndi ntchito yofunika kwambiri."** Mu Hadith sharif ina yanenedwa kuti: **"Mchitidwe wofunika kwambiri ndi Hajj-i-mabrur."** Hajj-i-mabrur imatanthauza Hajj yomwe imachitika popanda kuchimwa. Hadith sharif ina ikunena kuti ntchito yofunika kwambiri ndi **"Kuchita dhikr kwa Allahu ta'âlâ.** Ndipo inanso ikunena kuti ndi **"ntchito yomwe ikuchitika kawirikawiri ndipo mosadukizadukiza."** Kusiyanasiyana kwa yankho kunali chifukwa cha kusiyana kwa anthu omwe anafunsa funsolo komanso kusiyana kwa madera omwe anali. Komanso nthawi zosiyanasiyana zinkafuna mayankho osiyanasiyana. Mwachitsanzo, Jihad inali ntchito yabwino kwambiri m'masiku oyambilira a Chisilamu. [M'nyengo yathu ino, ntchito yofunika kwambiri ndikutsutsa anthu osakhulupilira ndi amene amatsutsa Madhhab. Izi tapange m'njira yosindikiza, kuwulutsa, ndi kufalitsa

chikhulupiliro chowonadi chophunzitsidwa ndi akadaulo a Ahl as-Sunnah. Anthu amene amathandizira akatswiri a jihadwa motere ndi chuma, popereka katundu kapena mwa kuthupi, adzakhala ndi gawo la thawab zomwe akatswiriwa amapeza. Ma Ayah ndi ma Hadithi sharif zikusonyeza kuti Swalah ndi y amtengo wapatali kuposa zakat kapena za chifundo za mtundu wina uliwonse. Koma ntchito yomwe ili ya bwino kwambiri kuposa kuchita Swalah, ndi kumpatsa chinachake wina amene watsala pang'ono kufa ndi kumupulumutsa ku imfa.]

6– Jabir bin Abdullah "radiyallâhu anh" anati: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Kulekanitsa kwa pakati pa munthu ndi kufur (kusakhulupilira) ndi kusiya Swalah."** Pakuti, Swalah ndi nsalu yotchinga munthu kuti asakumane ndi makafiri. Pamene chinsalu ichi chikuzimilira, kapolo (munthu) amatsikira ku ukafiri. Hadith sharif iyi yalembedwa mu **Sahih Muslim**. Hadith sharif iyi ikusonyeza momwe kuliri kuwopsya konyalanyaza Swalah. Ambiri mwa ma Sahabah kiram amanena kuti munthu amene wasiya Swalah popanda 'udhr amakhala wosakhulupilira (kafiri). Koma m'Madhhab a Shafi'i ndi Maliki uunthu ameneyo sakhala kafiri koma zimakhala wajib kumupha. M'Madhhab a Hanafi munthu wotere amayikidwa m'ndende ndikumenyedwa ndikusungidwa m'ndende mpaka atayambanso kuchita Swalah. Ubada bin Thabit "radiyallâhu 'anh" anati: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Allahu ta'âlâ watilamula (ife) kuchita Swalah kasanu tsiku lililonse.**

Ngati munthu achita udhu mwadongosolo ndi kumasunga nthawi yake komanso moganizira bwino za ma ruku ndi khushu ake, Allahu ta'âlâ akulonjeza kuti adzamukhululukira munthuyo. Iye sakuchita lonjezo lofanana kwa anthu amene sachita zimenezi. Adzawakhululukira kapena kuwazunza malinga ndi chifuniro Chake." Hadith sharif iyi yalembedwa ndi Imam Ahmad, Abu Dawud, ndi Nasa'i. Monga tawonera, ndikofunikira kukumbukira zofunikira za Swalah, monga ruku ndi sajda. Allahu ta'âlâ saphwanya pangano Lake. Ndithudi adzakhululukira Asilamu amene achita Swalah moyenera.

8– Abu Emama-i-Bahili "radiyallâhu anh" anati: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Chitani Swalah yanu kasanu pa tsiku! Kusala kwa mwezi umodzi (mu Ramadan)! Perekani zakat pa chuma chanu! Mverani malamulo a atsogoleri anu. Lowa M'munda wa Mbuye wanu."** Monga tikuonera, Msilamu amene amachita Swalah kasanu pa tsiku ndi kusala mu Ramadan ndi kulipira zakat pa chuma chake komanso kumvera malamulo oyenelera a olamulira a Chisilamu, omwe ndi ma Khalifa a Allahu ta'âlâ padziko lapansi,

adzalowa ku Mparadiso. Hadith sharif iyi inanenedwa ndi Imam Ahmad ndi Tirmuzi.

9- Burayda-i-Eslemi “radiyallâhu ’anh”, m’modzi mwa ma Sahabi olemekezeka, anati: Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” adati: **“Swalah ndi limodzi mwa ma pangano pakati panu ndi ife. Amene wasiya Swalah amakhala kafiri.** Monga tikuonera, munthu amene amachita Swalah amaweruzidwa kuti ndi Msilamu. Ngati munthu salemekeza Swalah ndipo sachita Swalah chifukwa sakuvomereza kuti ndi ntchito yake yayikulu, amakhala kafiri (wosakhulupilira).

Hadith sharif iyi yananedwa ndi Imam Ahmad, Tirmuzi, Nesai, ndi Ibni Maja, (anayi mwa akadaulo akuluakulu m’ma Hadith.)

10-Abu Zer-i-Ghifari “radiyallâhu ta’âlâ ’anh” akufotokoza kuti: Tsiku lina nthawi ya chilimwe Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” ndi ine tinatuluka. Masamba amayoyoka. Anathyola nthambi ziwiri za mtengo. Masamba a nthambizo onse anagwa nthawi yomweyo. **"Inu Aba Zer! Msilamu akachita Swalah chifukwa cha chisomo cha Allahu ta’âlâ, machimo ake onse amagwa ngati mmene akugwera masamba a nthambizi,”** adatero. Hadith Sharif iyi inanenedwa ndi Imam Ahmad.

11- Zayd bin Khalid Juhami anati: Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” adati**: “Msilamu akachita Swalah ya ma rakah awiri moyenera ndi khushu’, machimo ake akale adzakhululukidwa.”** Ndiko kuti, machimo ake onse ang’ono ang’ono adzakhululukidwa. Hadith sharif iyi yanenedwa ndi Imam Ahmad “rahima-hullâhu ta’âlâ!”.

12- Abdullah bin Amr ibni “radiyallâhu ta’âlâ ’anhuma” anati: Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anati: **"Ngati munthu achita Swalah, Swalah imeneyo idzakhala nur (kuwala) ndi burhan (umboni) ndipo idzamuchititsa kupeza chipulumutso. Ngati sakuteteza Swalah siyizakhala nur ndi burhan, kotero sadzapeza chipulumutso. Adzasungidwa limodzi ndi Qarun, Farawo, Haman, ndi Ubay Bun Khalaf.”** Monga momwe zikuwonekera, ngati Msilamu achita Swalah moganizira za fard zake, wajib, Sunnah, ndi adab, ndiye kuti Swalah zidzawachititsa kukhala mu nur pa tsiku lachiweruzo. Ngati sakuswali motere, adzakhala m'gulu la osakhulupilira omwe tawatchulawa pa tsiku la chiweruzo. Ndiko kuti adzakumana ndi chilango cha ukali ku Jahannama. Ubay bin Khalaf anali m'modzi mwa osakhulupilira a ku Makka. Mu Nkhondo Yopatulika ya Uhud, Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anamupititsa iye ku Jahannam ndi dzanja lake lodalitsika. Hadithi sharif iyi yalembedwa ndi Imam

Ahmad, Imam Bayhaki komanso ndi Darimi (Abdullah bin Abd-ur-Rahman Hafid Abu Muhammad).

13- Abdullah bin Shaqiq “rahima-hullâhu ta’âlâ!”, m'modzi mwa akuluakulu a Tabi'in, akunena kuti: "Sahabah kiram “radiyallâhu ’anhum” ananena kuti mwa ntchito zopembedza zonse ndi Swalah yokha imene ingachitise wonyalanyaza kukhala kafiri (mdani wa Allahu ta’âlâ). Izi zaperekedwa ndi Muhammad bin Isa Tirmidhi “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih”. Abdullah bin Shaqiq analongosola Hadith sharif iyi kuchokera kwa ma Sahabah monga Umar, Ali, Uthman, ndi Aisha “radiyallâhu ’anhum”. Iye anamwalira m’chaka cha108 AH.

14- Abu-d-derda “radiyallâhu ’anh” akufotokoza kuti: “Wokondedwa wanga anandiuza kuti: **“Ngakhale utang’ambidwa kapena kutenthedwa ndi moto, usam’phatikize Allahu ta’âlâ ndi chinthu china! Osasiya Swalah za fardh! Munthu amene wasiya Swalah za fardh amatuluka mu Chisilamu. Osamwa mowa. Mowa ndi makiyi a zoipa zonse.”** Monga tikuonera, munthu amene salabadira ndi kusiya Swalah za fardh amakhala kafiri. Munthu amene wasiya Swalah za fardh chifukwa cha ulesi sakhala kafiri; koma ndi tchimo lalikulu. Sikukhala kulakwa kulephera kuchita Swalah za fardh chifukwa cha imodzi mwa ‘udhr zisanu zimene Chisilamu chafotokoza. Mowa ndi za kumwa zina zonse zoledzeretsa zimayimitsa malingaliro a munthu. Munthu amene ali ndi maganizo oyipa amakhala wokonda kuchita zoyipa zilizonse.

15– Ali “radiyallâhu ’anh” akufotokoza. Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anati: **“Iwe” Ali! Pali zinthu zitatu zomwe siuyenera kuchedwetsa kuchita: Nthawi ya Swalah ikakwana chitani Swalah nthawi yomweyo!** Pomwe **Janaza** (Msilamu wakufa) **yakonzedwa** (kuyikidwa m'manda), **chita Swalah ya janaza nthawi yomweyo! mukapeza kufu wa mwana wanu wamkazi, (mamuna womuyenera) mukwatitse nthawi yomweyo!”** Hadith sharif iyi yanenedwa ndi Tirmidhi “rahima-hullâhu ta’âlâ!”. Swalah ya janaza iyenera kuchitika ngakhale mkati mwa nthawi zitatu zomwe zili makruh kuchita Swalah. (Nthawi zitatuzo zimatchedwa ‘Kerahat’[1]) [Monga momwe taonera, mkazi kapena mtsikana ayenera kukwatitsidwa kwa ‘kufu’ wake, kwa mamuna womuyenera iye. Kukhala ‘kufu’ sikutanthauza kukhala ndi chuma kapena kukhala ndi malipiro abwino. Kukhala kufu kumatanthauza kuti munthu akhale Msilamu wa Salih, wokhulupirira Ahl Sunnah, woswali kasanu tsiku lirilonse, wosamwa zakumwa

[1] Kerahat –nthawi zosaloledwa kuchita swalah iliyonse

zoledzeretsa, -womvera Chisilamu. Akhalae ndi ndalama zokwanira nafaqa (ndiko kuti, ayenera kukhala woti angasamale banja.) Makolo amene amafuna amuna okwatira ana awo kukhala olemera ndi okhala ndi nyumba, adziwe kuti akukokera ana awo akazi kuchionongeko ndi kuwaponya ku Jahannama. Ndipo mtsikanayo ayenera kuswali kasanu pa tsiku, asatuluke osadziphimba (kuyenda mutu ndi manja zili pa mtunda), ndipo asakhale malo awiri ndi mamuna yemwe ali na-mahram kwa iye, ngakhale atakhala mmodzi mwa achibale ake.]

16- Abdullah ibni Umar “radiyallâhu ’anhuma“ anasimba kuti: Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” adati: **"Allahu ta’âlâ amasangalala ndi anthu omwe amachita Swalah yawo nthawi ikangokwana. Ndipo amawakhululukira amene amachita Swalah mochedwa.”** Hadith sharif iyi yanenedwa ndi Tirmidhi “rahima-hullâhu ta’âlâ!”.

M'Madhhab a Shafi'i ndi Hanbali ndi kwabwino kuchita Swalah iliyonse kumayambiliro kwa nthawi yake. Madhhab a Maliki akuyandikiranso ku ganizo lomweli. Koma mu nyengo yotentha kwambiri munthu yemwe akupemphera yekha akhoza kuchedwetsa pemphero la masana. M'Madhhab a Hanafi ndi kwabwino kwambiri kupemphera Swala ya m'mawa ndi usiku mochedwa, komanso kuswali Swalah yoyamba ya masana (dhuhr) mochedwerako kutazizirirako m'miyezi yotentha. [Ndi bwino kusamala kuti Swalah yoyamba ya masana (Dhuhr) iswalidwe nthawi ya swalah ya yachiwiri ya masana (Asr) isanayambe molingana ndi qawl ya Tarafayn. Ndipo kuswali Asr ndi swalah ya usiku (Isha) nthawi ya Asr ndi ya Isha itayamba malinga ndi qawl ya Imam Azam Abu Hanifa. Anthu omwe ali ndi taqwa (kuopa Allahu ta’âlâ mowonadi) amakhala osamala pa chilichonse chimene akuchita.]

17- Umm-i-Farwa “radiyallâhu ’anha” akusimba kuti: Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anafunsidwa kuti ndi ntchito iti yomwe inali yabwino kwambiri. Iye adati**: “Ntchito yabwino kwambiri ndi Swalah yomwe imachitika kumayambiliro kwa nthawi yake.”** Hadithi sharif iyi yalembedwa ndi Imam Ahmad, Tirmidhi komanso ndi Abu Dawud “rahima-hullâhu ta’âlâ!”. Swalah ndi kupembedza kwa pa mwamba. Kumakhala kwa pa mwamba kwambiri kukachitika nthawi yake ikangoyamba.

18- Aisha “radiyallâhu ’anha” akufotokoza kuti: “Sindinamuone Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” akuchita Swalah mochedwa kawiri.

19- Umm-i-Habiba “radiyallâhu ’anha” akufotokoza kuti: Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” adati: **"Ngati kapolo wa Chisilamu (wa Allahu ta’âlâ) achita ma rak'at khumi ndi awiri a Swalah monga ntchito ya tatawwu[1] kuwonjezera pa Swalah za fardh za pa tsiku, Allahu ta’âlâ amamumangira nyumba yake ku Mparadiso.”** Hadithi sharif iyi yalembedwa mu Sahih Muslim. Monga tawonera, Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” amazitcha ‘tatawwu’ Swalah za Sunnah zonse zochitika limodzi ndi Swalah za fardh zatsiku lililonse, kutanthauza kuti ndi nafila (Swalah zowonjezera).

20- Abdullah bin Shaqiq “rahima-hullâhu ta’âlâ!”, mmodzi mwa akuluakulu a Tabi'in anati: Ndinamufunsa Hadrat Aisha “radiyallâhu ’anha” za Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” pa nkhani ya Swalah za tatawwu, zomwe ndi nafila (zowonjezera). Amayi wathu wodalitsikawa anati: “Iye amaswali ma rakaat anayi lisanafike gawo la fardh la masana (Dhuhr) ndi ma rakaat awiri atachita gawo la fardh; Ma rakat awiri atatha fardh ya swalah ya madzulo (Maghrib); ma rakat awiri atatha fardh ya swala ya usiku (Isha); ma rakat awiri asanaswali fardh ya swala mmawa. Nkhani iyi inanenedwa ndi Muslim komanso Abu Dawud “rahima-hullâhu ta’âlâ!”.

21- Aisha “radiyallâhu ’anha” anati: “Pa swalah za Sunnah zonse, Sunnah ya swala ya m’mawa ndi imene Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” amachita mokhazikika. Ndime iyi inalembedwa mu Sahih **Bukhari** ndi mu Sahih **Muslim**. Apa, Aisha “radiyallâhu ’anha” amatanthauza kuti Swalah za sunnah zomwe amachitira limodzi ndi Swalah za Fardh zisanu za pa tsiku ndi 'Swalah zongowonjezera'. [Imam Rabbani mujaddid-i-elf-i-thani Ahmad bin Abd-ul Ahad Faruqi Serhendi “rahmatullâhi ’alaih”, Kadaulo wamkulu wa Chisilamu, opambana wamphamvu kwambiri wa Ahl-i-Sunnah wolimbana ndi ampatuko ndi anthu opanda madhhab, mujahid amene adafalitsa chipembedzo chosankhidwa ndi Allahu ta’âlâ komanso yemwe adagwetsa bid'at, akunena motere m'kalata yake ya makumi awiri ndi chisanu ndi chinayi (29) m’gawo loyamba la bukhu lake lotchedwa **Maktubat**; bukhuli lilibe linzake mmafananidwe m'chipembedzo cha Chisilamu:

Ntchito zomwe Allahu ta’âlâ amakonda ndi ntchito za fardh ndi Zowonjezera zake (nafila). Ntchito Zowonjezera poyerekeza ndi fardh, zilibe phindu. Kuchita Swalah ya fardh imodzi mkati mwa nthaŵi yake yoyikidwa kuli kwamtengo wapatali kuposa kuchita machitidwe a

[1] M’bado wa Asilamu womwe unabwera pambuyo pa ma Sahabah a Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”

kulambira kopambanitsa kosalekeza kwa zaka chikwi. Mfundo imeneyi imagwira ntchito ku mitundu yonse ya kulambira kowonjezera monga Swalah, zakat, kusala, umra, hajj, dhikr, ndi fikr (kupemphera chamumtima). Kunena zoona, kuswali Swalah ya fardh ndi kuchita imodzi mwa Sunnah zake ndi adab, ndikofunika kwambiri kuposa kuchita nafila zina. Tsiku lina, pamene Emir-ul-mu'minin Umar-ul-Faruq "radiyallâhu 'anh" amapemphera Swala ya m'mawa pa Jama'at, anawona kuti munthu wina yemwe amamudziwa akusowa. Iye anafunsa Asilamu omwe analipo kuti chifukwa chiyani munthuyo kunalibe. "Iye amachita mapemphero a nafila usiku uliwonse. Ayenera kuti anagonetsa ndipo walephera kubwera kuno kudzachita jama'at," Iwo anafotokoza motero. Pamenepo Khalifa wodalitsikayu anati: "Zikanakhala zabwino akwambiri akanagona usiku wonse koma ndikudzaswali Swalah yake ya m'mawa pa Jama'at." Mutha kuona kuti pomwe mukuchita ntchito yopembedza ya fardh, monga gawo la fardh limodzi la Swalah zisanu za pa tsiku, kusunga imodzi mwa adab zake (kapena mendub) kapena kupewa imodzi mwa makruh kudzakhala miyanda-miyanda ya nthawi zapamwamba kwambiri kuposa kuchita chimodzi mwa zinthu zopembedza (zowonjezera pa wekha) monga dhikr, fikr, ndi muraqaba (kusinkhasinkha). Ndi zowona kuti zopembedza zowonjezera ndi zofunika kwambiri ngati zikuchitika potsata ma adab ndikupewa makruh.

Koma zowonjezera zimakhala zopanda phindu popanda fardh zake. Chimodzimodzi kulipira K100.00 ngati zakat, (yomwe ndi fardh kwa Asilamu**)**, ndi kwabwino kuposa kugawa masauzande a makwacha m'dzina la chopereka chongowonjezera (Sunnah). Ndithu, kuchita imodzi mwa adab (ya zakat) popereka 100 Kwacha imeneyo, kwa wa chibale wako wa pa mtima, [1] ndi kwabwino kwambiri kuposa kulambira kowonjezera. [Choncho, anthu amene akufuna kuchita Swalah pakati pa usiku (tahajjud) azichita atapanga qada Swalah zawo zonse. Malamulo a Allahu ta'âlâ amatchedwa **fardh**, ndipo zoletsedwa Zake zimatchedwa **haram**. Malamulo a Mtumiki wathu amatchedwa **Sunnah**, ndipo zoletsa zake zimatchedwa **makruh**. Zinthu zonsezi, pakuphatikizana, zimatchedwa **Ahkam Al-islamiyya**. Ndi fardh kukhala ndi mbiri yabwino ndi kumachitira anthu zabwino. Munthu amene wakana kapena kunyoza chimodzi mwa ziphunzitso za Ahkam Al-islamiyya amakhala **wosakhulupilira (kafiri), wopatuka (murtadd).** Munthu amene amakhulupilira Ahkam Al-islamiyya, amatchedwa Msilamu. Msilamu amene samvera Ahkam Al-islamiyya chifukwa cha ulesi amatchedwa Msilamu wa Fasiq. Msilamu wa fasiq yemwe waphwanya limodzi mwa malamulo kapena zoletsedwa adzapita ku

Jahannama. Palibe ntchito zabwino ndi Sunnah zomwe Msilamu wa Fasiq amachita zomwe zidzavomerezedwe, ndipo palibe thawab zomwe adzapatsidwe. Ngati munthu sapereka zakat, ngakhale ithakhala100 kwacha yeniyeniyi, ntchito zawo zina za chifundo sizidzalandiridwe. Sadzapatsidwa thawab iliyonse pa misikiti, kapena sukulu kapena zipatala zomwe amamanga ndi ndalama zawo kapena pa zopereka zawo zilizonse ku mabungwe achifundo. Swalah ya Tarawih yomwe wachita munthu yemwe sanaswali Swalah ya Isha sidzalandiridwa. Zopembedza zina zonse kupatula za fardh kapena za wajib zimatchedwa nafila (zowonjezera). Sunnah ndi mapembero owonjezera. Potengera tanthauzoli, munthu amene amachita qada Swalah ya Fardh ayenera kuchitanso qada ya Swalah ya Sunnah. Thawab (yopezeka) pa kuchita fardh kapena kupewa haramu ndi yochuluka kuposa thawab yomwe munthu amapeza pochita mapemphero owonjezera miyanda-miyanda. Munthu amene wasiya Fardh kapena wachita Haramu adzapachikidwa ku Jahannama. Kupembedza kwawo kwa zowonjezera sikungawapulumutse ku Jahannama. Kusintha kulikonse mmapembedzedwe kumatchedwa **bidah.** Kuchita bidah pochita mapemphero ndi haram ndipo kumawononga ntchito zakupembedza.

[Chonde onaninso mutu womwe ukunena za Adhan-i-Muhammadi!] Zanenedwa mu Hadith sharif kuti: **"Palibe ntchito zopembedza zochitika ndi munthu wochita bidah zomwe zidzalandiridwa."** Ngati munthu ali fasiq; mwachitsanzo, mkazi wake ndi ana ake a akazi amayenda osadziphimba bwino; kapena ngati akuchita bidah nati kugwiritsa ntchito chimkulitsa mawu popemphera; inu musaswali potsogoleredwa ndi iye. Musaswali Swalah ya jama'at yotsogolera munthu ameneyo ndipo musamumvere zoyankhula zake poti ndi zonyansa, kapena kuwerenga mabuku ake. Koma muyenera kukhala mwa chimwemwe ndi aliyense, bwenzi ndi mdani mofanana, ndi kuyankhula nawo mokoma mtima, musakangane ndi wina aliyense. Kwanenedwa mu Hadith sharif kuti: **"Zitsiru zisayankhidwe.**" Kupembedza kumawonjezera chiyero cha mtima. Machimo amadetsa mtima, moti siulandiranso fayz (mtendere). Ndi fardh kwa Msilamu aliyense pa yekha kuphunzira zofunikira za iman, fardh ndi haram. Kusadziwa izi si udhr yovomerezeka. Kuteroko ndi chimodzimodzi kusachita ngakhale munthu akuzidziwa.] Bukhu la **Maktubat** lili m'chinenero cha Chiarabu ndipo kumasulira kwake kukuthera apa. Hadrat Imam Rabbani anamwalira mu mzinda wa Serhend ku India mu 1034 [1624 A.D.].

Monga momwe zikumvekera kuchokera ku zomwe zalembedwa mpaka pano, Sunnah za Swalah zisanu za tsiku lililonse zili m'gulu la nafila (Swalah zowonjezera). Chifukwa choti zimachitika limodzi ndi Swalah za fardh ndi kusokelera zofooka za m'magawo a fardh omwe amachitika, ndi zabwino kwambiri kuposa za Swalah zina zowonjezera.

Msilamu yemwe sanachite Swalah ya fardh mu nthawi yake yoyikika popanda chifukwa chilichonse chomveka chotchedwa 'udhr amakhala kuti wachita tchimo. Izi zimakhala choncho ngakhale kuti iye amalemekeza Swalah kwambiri ndipo amayitenga kuti ndi ntchito yake yolemekezeka. Iye adzakhala pa modzi ndi Farawo ndi Haman ku Jahannama. Swalah zowonjezera zomwe ndi zigawo la Sunnah za Swalah zisanu za pa tsiku sizingamupulumutse ku tchimo lalikululo ngakhalenso ku chilango choopsa chomwe chingatsatire. Pa chifukwa chimenecho, ndi fardh kuchita qada ya Swalah za fardh zosiyidwa. Ndi tchimo lalikulu kuchedwetsa qada yawo. Utchimo ukukula ndi kuswana nthawi zonsewu uyenera kutha. Kuchita qada Swalah ndi fardh ndipo thawab zomwe zimapezedwa zimakhala ma sausande ma sausande kuposa kuchita Sunnah. Poti zikuloledwa kusiya Sunnah chifukwa cha udhr, Msilamu aliyense akuyenera kuchita qada Swalah za fardh zomwe sanachite popanda udhr m’malo mwa Sunnah za swalah zinayi za tsiku ndi tsiku. Chifukwa pali akadaulo a Chisilamu omwe amanena kuti Sunnah ya Swalah ya m’mawa ndi wajib, qada isachitike m'malo mwa Sunnah ya pemphero la m'mawa.

Potero adzachotsa tchimo lalikulu mwachangu pochita Qada Swalah zawo nthawi zonse. Qada za fardh zikachitika, Sunnah za Swalah zisanu za tsiku ndi tsiku zichitike mosalekeza. Ndithu, ngakhale liri laling’ono ndi tchimo kupitiriza osachita Sunnah popanda udhr. Ndipo munthu amene wanyoza Sunnah amakhala kafiri.

Ngakhale zili fardh kuchita Qada Swalah ya Fardh yomwe munaphonya mwachangu, (yomwe munalephera kuchita mu nthawi yake chifukwa cha 'udhr), akatswiri a Madhhab a Hanafi ananena kuti ndi zololedwa kuchedwetsa kuchita qada mpaka mutachita Sunnah (za swala zisanu za tsiku ndi tsiku), popeza sikulakwa kulephera kuchita Swalah ya fardh mu nthawi yake yoyikidwa ngati pali udhr.

Koma kuyankhula uku sakutanthauza kuti ndi kololedwa kuchedwetsa Swalah ya fardh yosiyidwa popanda udhr. Komanso kunena kuti ‘zololedwa’ sikutanthauza kuti ndi ‘wajib’ kapena ‘zabwino’. Pali zochitika zambiri zomwe zikunenedwa kuti ndi ‘zololedwa’ zomwe nthawi yomweyo zimanenedwa kuti ndi ‘makruh’. Mwachitsanzo, ndi kololedwa kupereka **sadaqa-al-fitr** kwa dhimmi

osakhulupilira, koma kutero ndi makruh. (Dhimmi ndi Munthu wakhala mdela logonjetsedwa ndi asilamu kuma anapatsidwa ufulu watsata chikhulupirira chake).

Muziswali ndipo musalole manja anu kukhudza haram;
Musayembekezere kukhala ndi moyo wautali, kapena dziko losatha!
Muswali kasanu pa tsiku mukadali achinyamata!
Zobzala pano mudzakolola m'dziko lotsatira.

Anthu awiri sadzakumbukira imfa ndipang'ono pomwe.
Wochita za haram ndi wosiya Swalah
Tsiku lina manja awa sadzatha kugwira;
Malirime omwe sanena kuti, "Allahu ta'âlâ," adzalephera kuyankhula!

KULIPIRA ZAKAT

Umboni wa mmalemba woti kulipira zakat ndi fardh ndi ayah 43 ndi 110 mu Surah Baqara.

Pali anthu khumi ndi awiri omwe ndi osaloledwa kulipira zakat:

Wamisala asalandire zakat; Msilamu wakufa, osagula kafen (nsanda); kafiri (munthu yemwe sali Msilamu); munthu wolemera; ma usul ako (makolo) ndi furu' (ana ako kumapita mmusi); mkazi wako; kapolo wako; mukataba wako [kapolo amene adzamasulidwe polipira mtengo wina wake]; mudebbera wako [kapolo amene adzakhale mfulu mwini kapoloyo akadzamwalira]. Zoti mkazi angapereka zakat kwa mamuna wake; iyi ndi nkhani yomwe ili mkati mwa zokambirana (za akadaulo a Chisilamu), koma siziyenera kuchitika.

Ngati mukuganiza kuti munthu wina si m'bale wanu koma ndikupezeka kuti iye ndi mmodzi mwa ana anu, kapena kuti ndi kafiri ngakhale inu mumaganiza kuti ndi Msilamu; anthu amenewa sioyenerera zakat; Koma ngati mwapereka Zakat kwa mmodzi mwa oterowo mosadziwa, sikuti abweze ayi. Anthu asanu ndi atatu otsatirawa ndi oyenera kupatsidwa zakat:

1– Munthu amene ali miskin m'mawu a Chisilamu. (Msilamu amene alibe chakudya chopitilira tsiku limodzi amatchedwa miskin.)

2 –Asilamu osauka omwe chuma chawo chili chosafika pa Nisab ya Qurban. (Nisab ndi malire; malire a pakati pa kulemera ndi umphawi m’mawu a Chisilamu. Nisab ya Qurban ndi sadaka yapadera yotchedwa Fitra zimasiyana ndi ya Zakat.)

3- Msilamu yemwe ngongole zamuthina;

4- Msilamu yemwe akutolera katundu wa zakat ndi ‘udhr (kukhala ngati malipiro ake);

5- Msilamu amene ali wosauka kumalo komwe ali (kuchilendo) pa nthawiyo, ngakhale kuti kwawo ndi olemera;

6- Msilamu amene wasauka ali paulendo wa ku Jihad kapena Haji;

7- Kapolo amene amayenera kulipira bwana wake ndalama kuti amasulidwe;

8- Omwe sali Asilamu otchedwa muallafa qulub (omwe asonyeza kuvomera kulowa Chisilamu koma chikhulupiliro chawo sichinakhazikike kwenikweni), amene kulibe lero.

Munthu amene ali ndi chuma choposa chakudya cha tsiku limodzi koma chocheperako ndi nisab amatchedwa ‘osauka’ (m’mawu a Chisilamu). Wogwira ntchito m'boma aliyense amene amavutika kuti apeze zofunika pa moyo wa banja lake, posatengera malipiro omwe amalandira, ndi oyenera kulandira zakat, ndipo sakuyenera kuchita Qurban kapena kulipira Fitra. Msilamu amene akuphunzitsa kapena kuphunzira maphunziro a Chisilamu ali oyenera kulandira zakat ngakhale ali ndi katundu kapena ndalama zomuthandiza kwa zaka makumi anayi. Ndalama za zakat sizingagwiritsidwe ntchito pomanga mzikiti, pa Jihad, kapenanso pogulira Msilamu wakufa sanda. Simungathe kulipia zakat kwa mwana wamng'ono wa munthu wolemera, kapena kwa makolo anu kapena ana anu kapena mkazi wanu. Ndi za thawab zambiri kulipira zakat kwa abale ako, apongozi ako (mkazi wa mwana wako), apongozi ako (amuna kapena akazi), azakhali ako (a kwa bambo kapena kwa mayi ako), amalume ako (a kwa bambo kapena kwa mayi ako). Msilamu wosauka ayenera kupatsidwa zakat yocheperako pofanizira nisab. Komabe, ngati ali ndi mkazi ndi ana, wonjezerani kuti alandire chochuluka (kuposa nisab) bola kuti m’banjamo pasapezeke wina wolandira zakat kuposa nisab ya Zakat. Zakat isaperekedwe kwa munthu amene amasakaza chuma chake kapena kuchigwiritsa ntchito m'njira ya haram. Ma Sayyid athanso kupatsidwa zakat popeza sangathenso kupeza magawo awo oyenera kuchokera ku ghanimat.

Pali zinthu zisanu ndi chimodzi zomwe munthu ayenera kukwaniritsa kuti kulipira zakat kukhale fardh (kwa iye):

1– Kukhala Msilamu;

2- Kukwanitsa zaka zakutha msinkhu;

3- Kukwanitsa zaka zotha kulingalira ndikuchita chiganizo payekha;

4- Kukhala mfulu;

5- Kukhala ndi chuma cha halal choperekera zakat chofika pa mlingo wa nisab ya zakat;

6- Kuti chuma chomwe munthu ali nacho chili chochuluka kuposa zosowa zake ndi ngongole zake.

Munthu amene sakulipira zakat yake kwa osauka pomwe zakat yakwanira kukhala fardh kwa iye ali ngati munthu amene ali ndi ngongole. Choncho ntchito zake za chifundo monga zothandiza ndi sadaka, pamwamba pompatsa thawab, zidzampatsa utchimo. Ndi fardh kwa iye kulipira zakat yake, kapena kulipira ngongole ngati ali nayo. Monga momwe kwalembedwera patsamba mazana asanu ndi limodzi ndi mphambu makumi atatu ndi zisanu (635) m'bukhu lachiwiri la **Hadiqa** ndi pa tsamba mazana makumi atatu mphambu makumi asanu ndi awiri ndi phambu zisanundi zinayi (1369) m'bukhu la **Bariqa,** ndi kosaloledwa kulipira [zakat ndi] sadaka kwa anthu amene amawononga ndalama zawo kumalo a haram kapena amene amangosakaza ndalama zawo. Pakuti ndi haram kuthandizira chinthu chomwe chili cha haram.

Sizoti munthu yemwe akulipira zakat adzapezabe phindu ndi zakat yake. Ngati mmodzi mamuna kapena mkazi apereka zakat kwa mnzake, phindu lake kwa woperekayo sikuti lidzatheratu. Monga tichitira pa ntchito yopembedza iliyonse, niyyah (cholinga) ndi yofunika popereka zakat. Chuma chochilipirira zakat chikuyenera kukhala chopyola ngongole za munthu komanso kupyola hajat asliyya (zofunikira kwambiri pa moyo wake), ndipo chiwerengero cha chuma chopyolacho chikhala mlingo wa nisab. Mlingo wa nisab wa golidi ndi 20 mithqal, [yomwe ndi yofanana ndi magalamu 96 kapena makobili 13.3 a zagolide.] Nisab ya siliva ndi ma dirham 200 [magalamu 672]. Kuti zikhale fardh kwa munthu kuti apereke zakat, chuma cha zakat chikafika pa mlingo wa nisab, chiyenera kukhala pa mlingo umenewo kwa chaka chimodzi cha hijra. Malinga ndi Imam Muhammad, ndi makruh kuchita chinyengo cha lamulo chotchedwa hila-ishar'iyya chaka cha (hijra) chisanathe powopera kuti zakat ingakhale fardh. Si makruh malinga ndi Imam Abu Yusuf. Woyambayo anafotokoza kuti:

Poti zakat ikangokhala fardh, ndi tchimo kusapereka. Ndipo ndi ta'at (kumvera) kupewa utchimo. Fatwa iyi ikugwirizana ndi matambasulidwe a Imam Muhammad. (Fatwa ndi kulongosola komaliza kumene katswiri wa maphunziro a Chisilamu wovomerezeka amayankha mafunso a Asilamu. Magwero a fatwa amawonjezeredwa m'menemo. Zomuyenereza munthu kuti akhale katswiri wamaphunziro a Chisilamu ovomerezeka zafotokozedwa m'mabuku athu, **Chikhulupiriro ndi Chislamu, The Sunni Path** and **Endless Bliss.**)

Katundu wa zakat amatanthauza katundu yemwe amawonjezereka, yemwe atha kuchulukitsadwa. Pali mitundu inayi ya katundu wa zakat: Nyama za miyendo inayi zomwe zimadya msipu kwa nthawi yoposa theka la chaka m'magulu osakanikirana, kapena zazikazi zokha, zomwe zimatchedwa **saima;** katundu wogulidwa ndi kugulitsidwa pochita malonda; ziwiya za golide ndi za siliva; zakudya zochita kulima mu nthaka. Anthu omwe ali ndi ziweto za mphongo zokha kapena a bulu kapena nyuru[1] zomwe zimadya zikungoziyendera sayenera kuzilipilira zakat; zakat si ili fardh kwa iwo. Pamene ziweto zazing'ono monga ana a ngamira, ng'ombe, nkhosa, mbuzi zili pamodzi ndi ziweto zazikulu, ziyenera kuphatikizidwa powerengera zakat. M'malo mopereka katundu amene ayenera kuperekedwa ngati zakat, ngati 'ushr, ngat kaffarah kapena ngati sadaqa fitr, ndi zololedwa kulipira ndalama zofanana ndi katunduyo. Koma m'Madhhab a Shafi'i ndi kosaloledwa kutero. Ngati chuma cha munthu chaonongeka koma chitakwana kukhala fardh kulipira zakat, sikowumirizidwanso kuti alipire, siyilinso fardh kulipira.

Chuma cha Msilamu wozindikira ndi woti watha nsinkhu chikatha chaka chimodzi (cha Chisilamu) chimafika pa mlingo wa nisab, ndipo ngati chuma chonse chili chake ndipo kuti anachipeza m'njira ya halal, zimakhala fardh kwa iye kulipira gawo linalake la chumacho kwa gulu limodzi kapena ochepa mwa magulu asanu ndi atatu a Asilamu; Kulipira kumeneku (komwe kuli kokakamiza) kumatchedwa **zakat**. Munthu amene adzapatsipidwa zakat ayenera kukhala Msilamu. Katundu wa munthu yense ndi katundu amene ali wotheka komanso wololedwa kugwiritsa ntchito. Katundu yemwe mukugula amakhala wanu pangano likachitika; koma siwanu kwenikweni popeza sizingatheke kumugwiritsa ntchito mpaka atakutulirani. Katundu wopeza molanda, kupondereza ena, mokakamiza, mwakuba, mwa chiwongola dzanja, mwa ziphuphu, potchova juga kapena kumupeza

[1] Nyuru ndi chiweto chobadwa kuchokera ku bulu wamamuna ndi hatchi yayikazi

poyimba chida choyimbira, poyimba kapena pogulitsa zakumwa zoledzeretsa, amatchedwa katundu wa **khabith**. Zakat siyilipilidwa pa katundu wa khabith. Pakuti, chuma chimenecho si chanu, chuma chanu chimatchedwa mulk. Ayenera kubwezedwa kwa eni ake, kapena kwa mlowam'malo wa mwini ngati mwiniyo ali malemu, kapena ngati palibe olowa mmalo chipite kwa Asilamu osauka. Ngati chuma (chomwe mwachipeza kudzera mu imodzi mwa njira za haram tatchulazi) chasakanizidwa ndi chuma china cha haram kapena ndi chuma chanu cha halal, chimasunduka mulk yanu, (chuma chanu); koma chidzakhalano **mulk habith**, (chuma cha khabith), chomwe ndi haram kumpatsa munthu wina kapena kuchigwiritsa ntchito, kotero zakat siilipilidwa pa chuma chotero chifukwa si mulk yanu kwa thunthu. Mutapepesa ndi kuwalipira eni ake kuchokera mu chuma chanu cha halal cha **zakat mithl** omwe ndi mtundu wina wa katundu wa khabith, kapena mtengo wake, ngati mithl yake palibe, kudzakhala halal kwa inu kugwiritsa ntchito mulk khabith ndipo mudzafunika kuwonjezera pa chiwerengero cha nisab yanu. Ngati mulibe chuma cha halal chokwanira kubweza ngongole zanu zimenezi, bwerekani kwa ena okudziwani ndipo mulipire. Ngakhale kuli zili haram kugwiritsa ntchito mulk habith kapena kumpatsa wina; ngati mukuyigulitsa kapena kuyipereka ngati mphatso, sizikhala haram kwa munthu amene wagulayo kapena amene walandira ngati mphatso. Ngati eni ake kapena olowa m'malo sakudziwika, kapena ngati chuma chosonkhanitsidwa kuchokera kwa anthu osiyanasiyana chasakanizidwa ndikukhala mulk khabith, mulk khabith zonse ziyenera kuperekedwa ngati sadaka kwa Asilamu osauka.

Ngati Msilamu wosauka akubweza chinthu chomwe wapatsidwa monga sadaka, ngati mphatso, ndiye kuti nzololedwa kwa amene waperekayo kulandira.

Golide ndi siliva sizigwiritsidwa ntchito mmene amakhalira golide kapena siliva yekhayekha. Ngati kuchuluka kwake kukuposa theka la zana, zakat ilipilidwe malinga ndi kulemera kwawo kutengedwe ngati maziko owerengera.

Ngati pali mitundu iwiri ya golide kapena siliva pa msika ndipo ikugwiritsidwa ntchito ngati muyezo, wotsukika kwambiri amatchedwa **jeyyid**, ndipo wotsalirayo amatchedwa **zuyuf.** Ngati kuyera kwawo kuli kosafika pa makumi asanu pa zana (50%) aliwonse ndipo akugwiritsidwa ntchito pa malonda, zakat zawo ziyenera kuperekedwa pamene mtengo wake ufika pa mlingo wa nisab wa golide kapena siliva, chimodzimodzi.

Ngakhale zokolola za ku munda zomwe zimamera ndi madzi amvula kapena a m'mitsinje zili zochepa, kaya ndi masamba kapena zipatso, zomwe sizichedwa kuwola ndi kuwuma, lipirani gawo limodzi mwa magawo khumi a izo kwa wogwira ntchito yotolela ushr[1][1]. Kenako mkuluyo amagulitsa 'ushr yomwe watolera ndikukapereka ndalamazo ku nthambi ya chuma yotchedwa **Bayt-ul-mal**. Pali mafotokozedwa a ukadaulo omwe aknena kuti ndi fardh kulipira ushr pa zipatso zikawoneka kapena zikacha kapena pokolola. Cha khumi chimaperekedwa ngati kuthirira kumachitika ndi mphamvu ya nyama kapena mpope kapena injini kapena makina ena. Chiyenera kulipilidwa musanachotse ndalama zirizonse zomwe munawononga. Sizololedwa kuti boma lipereke ushr ngati mphatso kwa mwini katunduyo kapena kumukhululukira kapena kuchotsera. Ushr imalipilidwanso pa uchi wofulidwa ku mapiri kapena ku mtunda ndi ushr.

Zakat siyilipilidwa kwa ma dhimmi. Atha kulipidwa sadaqa fitr kapena zinthu zolumbilira kapena za chifundo zina. (Ma Dhimi ndi anthu omwe si Asilamu omwe amakhala m'dziko la Asilamu.) Amene sali Msilamu komanso sali dhimmi sayenera kupatsidwa sadaka zomwe zili fardh kapena wajib kapena nafila (zophatikiza), posatengera kuti iye ndi musta'min kapena harbi. (Musta'min -si Msilamu ndipo akukhala mongoyembekezera m'dziko la Asilamu; harbi ndi amene akukhala m'dziko la anthu osakhala Asilamu.) Ngati Msilamu wosauka alibe ngongole, ndi makruh kumpatsa zakat yochuluka kapena yoposa nisab. Ngati wosaukayo ali ndi banja lolisamalira, mwachitsanzo, mkazi ndi ana, ndiye kuti ndi zololedwa kumupatsa ndalama zomwe kugawa kwake ndi kuchuluka kwa anthu a m'banjamo kudzakhala kocheperako pang'ono ndi nisab.

Ndizololedwa kugulutsa katundu polandira ma fulu omwe akugwiritsidwa ntchito pa msika. Fulu ndi ndalama ya chitsulo yosakhala golide kapena siliva, kapena ndalama ya pepala; chifukwa ndi chikhalidwe kugwiritsa ntchito izi ngati themen (mtengo wa chilungamo). Sizifunika kuti ichite kusankhidwa. Ngati ikukhala kasid (siyikugwiritsidwanso ntchito pa msika) malonda ochitika amakhala batil (osavomerezeka) malinga ndi Imam Azam Abu Hanifa "rahima-hullâhu ta'âlâ!". Koma malinga ndi Imameyn, omwe ndi Imam Abu Yusuf ndi Imam Muhammad "rahima-hullâhu ta'âlâ!", malondawo sakhala batil. Ndalama yofanana mu mphamvu idzaperekedwa. Ngati fulu (ndalama ya chitsulo kapena ya pepala) ikukhala kasid, kuti

[1] Ushr is 10% ya chopereka pa zokolola za munda

siyikugwiritsidwanso ntchito pa msika, koma itabwerekedwa, Fulu yochuluka ngati mulingo unabwerekedwawo udzaperekedwa, malinga ndi Imam Azam. Koma malinga ndi Imameyn golide kapena siliva yomwe mphamvu zake ndi zolingana ndi mphamva ya zobwerekedwa idzabwezedwa. Kugula ndi kugulitsa pogwiritsa ntchito fulu yomwe siyikugwiritsidwa ntchito imafinika tayin ya fulu, kuonetsa. Chuma chomwe chapangidwa tayin chiri ndi zizindikiro za taayyun (kusonyeza).

Izi zikutanthauza kuti ngati chuma china chaonetsedwa, chuma chomwecho chiyenera kubwenzedwa mmalonda omwe akuchitika. Simungapereke chofananira. Tiyerekeze munthu akupereka siliva wolemera dirham imodzi kwa wosintha ndalama ndipo ndi kupempha wosintha ndalamayo kuti amupatse theka la dirham ma fulu ndipo theka lotsalalo amupatse siliva wolemera habba kupuwukako pa theka dirham; Malonda amenewa ndi fasid. Ndi nchitidwe wa fasid kugulitsa theka la dirham ya siliva polandira siliva wopewuka pa theka la dirham. (Habba ndi muyezo wolemera ngati njele ya bale.) Ngati atanena "Ndipatseni ma fulu olemera theka la dirham ndi siliva wolemera mochepera ndi habba pa theka la dirham posinthana ndi dirham imodzi ya silivayi." Ndiye kuti malonda onsewo ndi sahih. Poti silver yemwe akulumera motsikirapo ndi habba adzakala atagulitsidwa ndi silve wofanana kulemera ndipo theka la dirham ya ma fulu adzakhala atagulitsidwa ndi siliva wolemererapo ndi habba kuposa theka dirham ya silva. Ngakhale kuti fulu ndi siliva woperekedwa ndi wosiyana mmalemeredwe, malondawa ndi ovomerezeka poti akusiyana mtundu wa katundu.

Zanenedwa m'bukhu lotchedwa **Bedayi'us-sanayi' fi tertib-ishsherayi':**[1] "Katundu woperekedwa monga zakat ayenera kukhala wamtundu umodzi ndi katundu akuperekedwera zakatyo. [Sizololedwa kulipira wosauka zovala, nsapato, tirigu, mafuta, kapena zinthu zina zofananira nazo m'malo mwa golide.] Chuma cha zakat ndi ayn kapena deyn.

Zoyenera zakat yomwe ili ayn ndi zoyezeka, poyeza kulemera kwake kapena kuchuluka kwake kapena chinthu chosayezedwa. Ngati chiri chinthu chosayezeka ndiye kuti ndi ziweto za saima kapena malonda a uruz, (katundu osati ziweto). Ngati zili ziweto za saima;

[1] Yolembedwa ndi Abu Bakr bin Mes'ud Alauddin Shashi Kashani "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih"(d. 587 [1191 AD], Aleppo) ngati ndemanga ya buku lotchedwa Tuhfa-t-ul-fuqaha, limene linalembedwa ndi mphunzitsi wake Alauddin Muhammad bin Ahmad Samar-kandi "rahmatullâhi 'alaih"(d. 540 [1145 AD]).

pomwe chiwetocho chikulipiridwa zomwe zatanthauziridwa mu Nass (ayah ndi hadith sharif momveka) chiweto cha msinkhu wapakatikati chimalipilidwa. Pamene chiweto chochepera nsinkhu chikuperekedwa, kusiyana kwake ndi chija chapakatikati kumakwanilisidwa powonjezera golide kapena siliva. Pamene mtengo wa chiweto uyenera kuperekedwa, mtengo wa chiweto chapakatikati umalipiridwa. Pamene mtengo wa yocheperapo waperekedwa, kusiyana kwa mtengo ndi mtengo wa chapakatikati chija kumakwanilisidwa powonjezera golide kapena siliva. M'malo mwa nkhosa ziwiri za nsinkhu wapakatikati, ndizololedwa kulipira nkhosa imodzi yomwe mnofu wake ungafanane kuchuluka pa mtengo ngati ziwiri za nsinkhu wapakatikati. Poti mtengo umaganiziridwa ndi katundu yemwe angakhale ndi faiz (chingola dzanja). Pa katundu wa malonda gawo limodzi mwa magawo makumi anayi a chuma zanenedwa mu Nass limalipilidwa ngati zakat. Nati katundu wina wa mtundu womwewo akulipilidwa, malipiro akhale katundu wapakati kapena wotsika pophatikizapo chothetsera kusiyana kwake (mumtundu kapena mtengo). Pakuti, 'uruz amatanthauza katundu wosayezedwa ndi kulemera kapena ndi mphamvu. Ndi katundu wa uruz, kusiyana kwa kuchuluka sikumachititsa faiz. Mwachitsanzo, masuti awiri a zovala zotsikirako mtengo atha kuperekedwa m'malo mwa suti imodzi yokwera mtengo. Pamene katundu wina wa mtundu wosiyana akulipiridwa, kulipira chinthu chotsika mtengo chomwe chili fardh kumafuna kuonjezera choti chithetse kusiyanako. Pamene chuma cha zakat ndi chinthu choyesedwa ndi kulemera kapena mphamvu, gawo limodzi mwa magawo makumi anayi a katunduyo amalipidwa. Ngati munthu alipire chuma cha zakat cha mtundu wina, ayenera kulipira ndalama zofananira ndi mtengo wake. Ngati wina alipire katundu wina wa mtundu womwewo, amalipira ndalama zofanana, osati kuchuluka kwa mtengo womwewo. Izi ndi malinga ndi Shaikhayn, (Imam A'zam Abu Hanifa ndi wophunzira wake Imam Abu Yusuf,) "rahima-hullâhu ta'âlâ!". Mwachitsanzo tiyerekeze mtengo wa 200kg tirigu wabwino ndi 200 dirham siliva, ndikololedwa kulipira 5kg tirigu wochepa ngati zakat yake. Momwemonso, m'malo mopereka ma dirhamu asanu a siliva wa jeyyid (wa pa mwamba) monga zakat ya ma dirhamu 200 a siliva wa jeyyid, ma dirhamu asanu a siliva wa zuyuf (otsikirapo) atha kulipiridwa. Lamuloli limagwira ntchito pa nkhani zokhudza nazr.

"Golide ndi siliva ndi **Milingo** (milingo yokhazikika, mitengo). Zinalengedwa ngati milingo. Golide ndi siliva sizingagwiritsidwe ntchito ndi cholinga chokwaniritsa zosowa za anthu. Izi ndi njira

yogulira zosowa zofunika. Pomwe zinthu zina, zalengedwa kuti zitha kukhala mlingo ndi kugwiritsidwa ntchito pa zokha." Apa tikumaliza kumasulira kwathu kuchokera ku **Bedayi'**. Zinthu zomwe munthu amafunikira kuti akhale ndi moyo wabwino komanso mu njira yovomerezeka ndi Chisilamu zimatchedwa **zofunika kwambiri.** Zinthu zofunika kwambiri zimasintha, malinga ndi mayiko, chikhalidwe komanso thawi zomwe anthu akukhala. Zinthu zochulukirachulukira zomwe sizifunikira pa moyo wabwino zomwe zimagwiritsidwa ntchito ngati zosangalatsa kapena zokongoletsera kapena kukopa chidwi zimatchedwa za **manyado** (zinat). Golide ndi siliva sizili zina mwa zofunika; ndi zinthu zokongola. Kugwiritsa ntchito zinthu zozikongoletsa zomwe zili Mubah (zololedwa) ndi kololedwa kwa amuna ali pa khomo ngakhalenso popita koyenda, kkoma akazi ndi kololedwa pokhapokha ali pa nyumba.

Monga tikuwonera, ndalama ya chitsulo kapena pepala (ma fulû) zomwe zilipo nthawi zonse ndi katundu wa malonda. Mtengo wake ukafika pa mtengo wa nisab potengera pa maziko a ndalama zochepa za golide zomwe zimagwiritsidwa ntchito pa msika, zimakhala farz kuzilipira zakât. Pakuti, kuchuluka kwa nisâb ya katundu wa malonda kumawerengedwa ndi golide kapena siliva makamaka chomwe chikugwiritsidwa kwambiri pa malonda; malinga ndi Imameyn (Imam Abu Yusuf ndi Imam Muhammad "rahima-hullâhu ta'âlâ!", ophunzira awiri odziwika bwino a Imam A'zam Abu Hanifa "rahima-hullâhu ta'âlâ!"). Ndipo zakat pa katunduyo imaperekedwa ndi ndalama, (golide kapena siliva) potengera mtengo wake wawerengedwa kapena gawo limodzi mwa magawo makumi anayi a katunduyo aperekedwa. Munthu wosauka amachigwiritsa ntchito katunduyo pa zosowa zake zofunika. Fulu imatanthauza ndalama zina osati golide ndi siliva. Ma Fulu amakhala makobili a zitsulo osungunulidwa kuchokera ku kopa kapena bronze kapena zosakaniza zina kapena ndalama pepala. Izi zikutanthauza kuti ndalama ya pepala ndi fulu. Ziyenera kulipiliridwa zakat. Koma mosiyana golide ndi siliva, Izo **zilibe mtengo weniweni** okhazikika. Ndi **mtengo wadzina**. Ndi mtengo woyikidwa ndi maboma. Iwo akhoza kusintha zochita zawo mmene angafunire. Mtengo wodziwika (wa fulu) wachoka, siyingakhalenso mulingo (wa mtengo). Zikatero siyingagwiritsidwe ntchito ngati chuma cha zakat. Ibni 'Abidin akuti: "Mtengo wa katundu wa malonda umawerengeredwa ndi ndalama za golide kapena siliva zomwe zapangidwa kukhala mulingo wa ndalama zomwe zimagwiritsidwa ntchito nthawi zambiri pa zamalonda. Tiyerekeze kuti mtengo wa katundu wina ndi wofanana ndi ma dirham 240 a siliva akawerengedwa ndi siliva komanso ndi ma

mithqal 20 a golide akawerengedwa ndi golide; uku ndi kuchuluka kwa mtengo wa nisab ku mbali zonse ziwiri; koma chumacho chiyenera kuyesedwa pa maziko a siliva.

Pakuti mwini chuma adzapereke ma dirham 6 a siliva kapena theka la mithqal ya golide, yomwe ili yolingana ndi mtengo wa ma dirham 5 a siliva, ndipo izi sizidzachita bwino kwa wosauka (opatsidwa zakatyo). [Pakuti, ma mithqal 20 a golide ndi ma dirham 200 a siliva akusonyeza nisab yofanana (mlingo wake), mtengo wake ndi wofanana.] Kobili la golide lomwe limalemera mithqal imodzi limatchedwa **dinar**. [Ma lira onse a golide a ku Turkey amalemera mithqal imodzi ndi theka, omwe ndi magalamu 7.2, iliyonse.] Ndi wajib kulipira zakat pa ndalama yotchedwa fulus [mu golide kapena siliva] zomwe zagwiritsiridwa ntchito pa kuŵerengera kuchuluka kwa nisab. Izi zikutanthauza kunena kuti nisâb ya ndalama ya mapepala iyenera kuwerengedwa ndi yomwe ili ndi mtengo wotsika wa lira ya golide yomwe imagwiritsidwa ntchito pa zinthu zamalonda, ndipo zakat yake iyenera kulipidwa ndi golidi. Ndi wajib kulipira zakat pa ndalama yotchedwa fulus [mu golide kapena siliva] zomwe zagwiritsiridwa ntchito pa kuŵerengera kuchuluka kwa nisab. Pakuti, siliva sakugwiritsidwanso ntchito ngati ndalama tsopano, zakat ya ndalama ya pepala ilipidwa muzitsulo, mwachitsanzo golide, yomwe akugwiritsidwa ntchito powerengera (kuchuluka) kwa nisab. Gawo limodzi mwa magawo makumi anayi a mtengo wake siyingalipidwe ndi pepala. Poti ndalama ya pepala payokha sizingagwiritsidwe pa zinthu zofunika. Chingakhale chinyengo kugwiritsa ntchito ndalama ya mapepala m'malo mwa mapepala omwe alipo akale. Ndipo chinyengo ndi haram. Komanso sikuloledwa kulipira ndalama ya pepala ngati zakat kuti zigwiritsidwe ntchito ngati ndalama. Pakuti, pali golide, ndalama za mtengo wapatali komanso zenizeni, zomwe ziyenera kukondedwa nthawi zonse popereka zakat.

Golide akhoza kulipidwa, osati mu ndalama zokha komanso mu njira ina iliyonse. Golide mapezeka nthawi zonse komanso kulikonse. Tiyerekeze kuti Msilamu sangapeze golide mu mzinda umene amakhala; iye amatumiza ndalama za mapepala kwa bwenzi lake lomwe likukhala mu mzinda umene zinthu za golidi zikugulitsidwa ndipo amupemphe kuti agule golidi ndi ndalamazo ndi kulipira zakat m'malo mwake. Ndi zololedwa kwa iye kulipira ngongole yake ndi ndalama za pepala pambuyo pake. Kuthekera kumeneku kolipira zakat ndi ndalama ya pepala, kusakhale choyenereza kukana kulipira golide ndi cholinga chofuna kulipira ndalamaya pepala ya komwe muli. Musagwiritse ntchito njira iyi muli ndi golide pongofuna kukanira

malamulo omwe anenedwa m'mabuku a Chisilamu a Fiqh. Anthu amene amanyalanyaza kutsatira ziphunzitso za Chisilamu zopezeka m'mabuku a Fiqh ndi kumayesayesa kuchita za chipembedzo molingana ndi malingaliro awo, a momwe iwo akumvera ma ayah a mu Quran, amatchedwa anthu a **la-madhhabi**, (anthu opanda Madhhab) kapena **ampatuko.**

Yankho lathu kwa anthu ampatuko amenewa liyenera kukhala lotere: "Sindikuchita mapemphero anga molingana ndi zomwe mwalemba zopotoloza za Qur'an al-kareem ndi Hadith sharif, koma mogwirizana ndi zomwe ma Imam (a Madhhab anayi) ankamvetsetsa ndi kufotokozera." Mabuku ophunzitsa kumvetsetsa za ma Imams a Madhhab "rahima-hullâhu ta'âlâ" amatchedwa **mabuku a Fiqh**.

Kitab-ul-fiqh 'alal-madhahib-il-erbe'a, lokonzedwa ndi gulu la muderrisin (mapulofesa) a madrasa ku yunivesite ya **Jami'ul edhher** motsogozedwa ndi Prof. Abd-ur-Rahman Jeziri, amapereka maphunziro onse a Fiqh m'magulu anayi osiyana, gulu lililonse la ziphunzitsozi limakamba za amodzi mwa Madhhab anayi. Buku lonselo, lomwe lili m'magawo asanu, linasindikizidwa ku Cairo mu 1392 hijri [1972 A.D.]. Pa mutu wake wa 'Zakat ya awraq maliyya (ndalama za pepala)' bukhuli likunena motere: "Akadaulo a Fiqh ananena kuti ndi koyenera kulipirira zakat awraq-i-maliyya (ndalama za pepala). Poti zikugwiritsidwa ntchito m'malo mwa golide ndi siliva pa malonda. Nthawi zonse amatha kusinthanitsa ndi golide kapena siliva mosavuta. Ndi zosavomerezeka kwa munthu amene ali ndi ndalama yambiri ya pepala kuti asawonjezere mtengo wake ku golide ndi siliva wake pamene akuwerengera kuchuluka kwa nisab ya zakat. Ndi choipa kwambiri kusalipilira nkomwe zakat ndalama ya pepala. Pachifukwa chimenecho, Akatswiri Fiqh m'ma Madhhab atatu anagwirizana kuti ndikofunikira kulipira zakat pa ndalama za pepala. Madhhab a Hanbali okha ndi omwe akusiyana ndi kumvana uku. Akatswiri a Madhhab a Hanafi ananena kuti ndalama za pepala ndi **deyn-iqawi** ndipo zimatheka kusinthana ndi golide ndi siliva mwakufuna komanso msangamsanga. Iwo anaonjezeranso kuti pa nkhani ya zakar, iyenera kulipilidwa mosazengereza. Pakuti, kulipira zakat pa ngongole yomwe nthawi yobweza yakwana kumakhala fardh pamene ikulandilidwa mu golide. Ngakhale kuti zakat imakhala fardh ngongole isanalandilidwe, sizikhala fardh kuyilipira ngongleyo isanalandilidwe." Zikatero, muli ndi zisankho ziwiri: Mungathe kudikira mpaka mutalandira ndipo ndi kulipira zakat ya zaka zomwe zawerengedwa; kapena mupereke zakat chaka ndi chaka popereka

golide wa ‘ayn ndi siliva yemwe muli nayo. Simungathe kugwiritsa ntchito malonjezano omwe muli nawo (chikalata cha umboni kuti wina ali nanu ngongole) kulipira zakat ya golide yemwe mukuyembekezera. Mukatolera golidi ndi siliva zolembedwa pa chikalata cha malonjezo kuchokera kwa wangongole, zimakhala farz kwa inu kulekanitsa gawo limodzi mwa magawo makumi anayi pa chaka chilichonse chapita ndikugawa kwa osauka.

Choyenera kuchita ndi kugula ndalama za golide zotsika mtengo kuchokera kwa wosintha ndalama, pogwiritsa nthchito gawo limodzi mwa magawo makumi anayi a ndalamazo. Ndipo pereka makobili omwe mudagula, mphete zagolidi kapena zibangili zomwe ndi zolemera zofanana ndi ndalamazokwa osauka.

Ndi zosaloledwa kumukhululukira wongongola wako pa ngongole yake pochotsera ku Zakat yomulipira m’njira yoti zichotserane zakat ndi ngongoleyo, kotero kuti iye asakubwezereni ngongole yanu ndipo inu musamulipire Zakat. Muyenera kulipiradi zakat kwa munthu wosauka, ndipo pambuyo pake adzabweza ngongole yake pobweza zomwe wapatsidwa. Kwa wobwereketsa amene sakukhulupilire kuti wobwerekayo adzabweza zimene walipidwa, pali njira ina imene yaganiziridwa m’chigawo chomaliza cha gawo la chisanu ndi chimodzi m’buku la **Fatawa-yi-Hindiyya.** Ganizoli limati: “Wobwereketsa apeze munthu amene amamukhulupilira ndipo amuonetse kwa wobwereka, nati, ‘Mulole munthu uyu kukhala kazembe wanu kuti atenge zakat imene ndidzakulipirani, ndipo kuti iye adzandibwezela ngongole yomwe inu muli nane.’ Pamenepo wobwereka wosaukayo amamphanga munthu ameneyo kazembe wake. Munthu ameneyo akatenga zakat, chuma chimene watengacho, (monga zakat) chimakhala cha wosaukayo. Kenako adzapereka chumachi kwa wobwereketsayo ngati gawo lobwezera ngongole, ndipo potero ngongole ya wosaukayo idzakhala itabwezedwa. Tiyerekeze kuti munthu wosauka ali ndi ngongole kwa anthu awiri osiyana ndipo m’modzi mwa anthuwo akufuna kuti amuchotsere ngongoleyo wosaukayo pomulipira zakat monga momwe iliri ngongole ya wosauka; wongongozayo amapereka kwa wosauka uja ngongoleyo ngati chopereka. Akatero ndiye kuti amuchotsera munthu wosauka ngongoleyo mwa njira ya halal. Pambuyo pake wosauka amabweza (golide adamupatsa monga) Zakaat kwa wolemerayo monga mphatso. Kapena wosauka amabwereka golide wofanana ndi ngongole yake kwa munthu wina ndikuyipereka ngati mphatso kwa munthu wolemera, yemwe nayenso

amabweza golideyo kwa wosauka ndi cholinga chofuna kumulipira zakat, ndi kumuchotsa wosauka pagulu la angongole ake, ndiko kuti, amukhululukira ngongole yake. Pambuyo pake wosauka amabweza golide yemwe adalipidwa monga zakat (ndi wolemera) kwa wobwereketsa golideyo. Katundu oyenera kuperekedwa monga zakat [kapena katundu wolonjezedwa] sangagwiritsidwe ntchito pochita zinthu zopembedza kapena za chifundo (m'malo molipira zakat kapena kulipira katundu wolonjezedwa). Pochita zimenezi mupereka zakat kapena cholonjezedwa kwa munthu wosauka amene mukumudziwa, ndipo munthuyo ndi yemwe angathe kugwiritsa ntchito pa za chifundo." Pomwe tidzimaliza kuchokera ku zitsanzo izi, kutha kulipira zakat ndi ndalama ya pepala, mumabwereka zinthu za golide zodzikongoletsera zomwe kulemera kwake ndi kofanana ndi ndalama za golide zomwe mukufuna kulipira m'malo mwa ndalama ya pepala kuchokera kwa mkazi wanu kapena kwa mmodzi wa anzanu. Inu muwapatse golideyo ndi cholinga cha Zakat kwa mmodzi mwa omwe mumawadziwa bwino kapena achibale. Tsopano mwalipira zakat pa ndalama yanu ya pepala (popereka zinthu za golide zofanana kulemera kwake ndi ndalama zagolide zomwe zili ndi mtengo wofanana ndi ndalama zowerengetsera za pepala zomwe ziyenera kulipiridwira zakat.

Pambuyo pake wosaukayo amapereka golideyo monga mphatso kwa inu, ndipo inunso mudzabweza ngongole yanu pobweza zinthu za golidezo kwa wobwereketsawo. Popeza zakat yalipidwa, inuyo, wolemeranu, perekani zina mwa ndalama za pepala zomwe muli nazo komanso zomwe mwasunga ndi cholinga chopereka zakat kwa wosauka. Mutha kugwiritsa ntchito zotsalazo pochita za chifundo zili zonse zomwe mukufuna. Nayenso wosauka akafuna kupeza gawo la thawab lomwe sadaka ingamupezetse, akugulitsani golide yemwe analandira ngati zakat. Pambuyo pake amakubwezerani ndalamazo ndikukuyikani wachiwiri wake kuti mupereke za chifundo m'malo mwake.

Sayyid Abd-ul-Hakim Arwasi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" (1281 [1865 AD], Başkale, Van, Turkey–1362 [1943], Ankara), katswiri wa ziphunzitso za Madhhab onse anayi, anati: "Mtengo wa ndalama ya pepala ndi mtengo wongotchula. Akautsitsa, imatsikanso mtengo wake. Choncho, ndi kosaloledwa kulipira fitra kapena zakat mu ndalama za pepala. Zakaat yomwe mudapereka mu ndalama za pepala m'mbuyomu zikhale Qada (kubwerezanso,) mwa njira ya dawr ndi

golide. Kupembedza kulikonse komwe munagwiritsa ntchito ndalama ya pepala kupatula Hajj, mutha kuchita qada mwa njira ya dawr."

Zikunenedwa motere mu **Durr-ul-mukhtar:** Ngati ma Baghi, Asilamu ogalukira boma ndi kulanda ulamuliro, ndi olamulira a Chisilamu opondereza asonkhanitsa Zakat za nyama ndi zakat (zotchedwa 'ushr) za zakumunda ndikuzigawa molingana ndi m'malo olamulidwa ndi Allahu ta'âlâ, chuma chosonkhanitsidwacho (kuchokera kwa Asilamu) chimasanduka zakat (ndi ushur) za Asilamuwo. Koma ngati katunduyo waperekedwa popanda kutero m'malo ena, katundu wosonkhanitsidwawo sadzayimira zakat kapena 'ushr (chakhumi). Eni chumacho adzayenera kulipira zakat kapena ushr poperekanso kwa Asilamu osauka. Ngati akuluakulu omwe tawatchulawa atolera zakat kuti agulitse katundu wakeyo pa malonda ndi kutolera zakat kuti apeze ndalama, kutero siimayimira zakat, malinga ndi unyinji wa akatswiri a Chisilamu. Fat'wa zomwe zinaperekedwa zimagwirizana ndi ijtihad yawo. Malinga ndi akatswiri ena a Chisilamu, popeza olamulira opondereza omwe amasonkhanitsawo ndi Asilamu komanso kuti chuma chomwe anasonkhanitsacho ndi chawochawo anthuwo, iwo adzatengedwa ngati anthu osauka, ndipo chumacho chidzalipiridwa kwa iwo ndi niyyah (cholinga) ya zakat chidzayimira kukhaladi zakat."

Kufotokoza kwa **Ibni Abidin** pa nkhaniyi kuli motere: "Lamuloli limagwiranso ntchito pa katundu ndi ndalama zomwe zimasonkhanitsidwa monga msonkho kapena ntchito kapena m'matchulidwe ena aliwonse. Mtsutso wodziwika bwino wa akatswiri woti katundu wosonkhanitsidwa ndi anthu amenewa sangakhale zakat ngakhale kuti cholinga ndi chimenecho ndi sahih (wovomerezeka). M'mawu ena, olamulira ankhanza a Chisilamu alibe ufulu wotolera zakat pa katundu wa anthu." Zoti fat'wa iyi ikugwirizana ndi ijtihad zalembedwa m'mawu ofotokozera a **Tahtawi** m'bukhu lomwe tatchulali. Monga taonera, zakat yolipira nyama ndi 'ushr (zokolola) idzakhala sahih (yovomerezeka mu Chisilamu) pokhapokha ngati boma lomwe lizitolera ndi boma la Chisilamu ndipo zikuperekedwa kwa anthu omwe ali ndi gawo kuchokera ku nthambi zinayi za chuma za dziko zomwe zanenedwa zotchedwa **Beyt-ul-mal**. Palibe msonkho uliwonse womwe umalipiridwa ku boma, malinga ndi akatswiri ambiri a Chisilamu, ungayimilire zakat pa katundu kapena ndalama. Pali lipoti la ukadaulo lomwe likunena kuti zingakhale zololedwa pokhapokha boma lidziwike kuti ndi boma la Chisilamu ndipo katunduyo ndi

ndalama zotolerazo zikuperekedwa ndi cholinga cha zakat. Koma gwero la lipotili, ndi da'if (lofowoka).

Bwera, o m'bale wanga, khala ndi cholinga ndipo thetsa vutolo!
Moyo wako ndi wamtengo wapatali, musawuwononge pa zinthu zopanda pake!

Chinjiriza mtima wako ku zilakolako za Nafs!
Lolani mkati mwako, monga kunja kwako, kukhala koyera!

Golide akasakanizidwa ndi mkuwa,
Kodi wosintha ndalama adzalandira mokondwera?

Osadzikweza ndi dipuloma ako a sukulu ya pamwamba!
Ganizani usanayankhule, kuopera kuti mungatengeke ndi zolaula!

Pezani munthu wa ma'arif (ophunzira) ndipo mumumvetsere!
Kuti kuchokera mu Haqq (chowonadi) mupeze chifundo chochuluka!

Pitani kunyanja ya Haqiqat ndi kudumphira m'menemo,
Ndipo bweraniko ndi chinthu chapamwamba kwambiri!

Musalole mbuli yophunzira kukusokeretseni!
Akatswiri oyambilira akuwonetsani njira ya chiyero!

KUSALA kapena KUFUNGA

Pali ma Fard atatu mu kusala:

1- Kuchita niyyah (cholinga)

2- Kuchita niyyah pakati pa nthawi yoyambira kusala mpaka kumapeto kwake.

3- Kupewa zowononga kusala nthawi mu nehar-i-shar'i (nthawi ya usana pa Chisilamu), yomwe imatha pakulowa kwa dzuwa. Nthawi ya imsak ndi pamene kuyera kotchedwa fajr-i-sadiq kumaonekera mphepete mwa nzere wa ufq-i-zahiri (chizindikiro chowonekera). Munthu amene wapewa zowononga kusala mpaka madzulo koma osachita niyyah (cholinga) yosala mu nthawi yokhazikika ndi Chisilamu; munthu ameneyo sanasale tsiku limenelo. Adzayenera kuchita qada ya kusala kwa tsiku limenelo lokha.

Pali zinthu zisanu ndi ziwiri (7) zomwe ziyenera kukwaniritsidwa kuti Kusala (kufunga) kukhale farz kwa munthu:

1- Kukhala Msilamu. 2- Kukwanitsa zaka zakutha nsinkhu. Kusala kwa mwana ndi sahih.

3- Kukwanitsa zaka zotha kuzindikira. 4- Kwa Msilamu wokhala ku dar-ul-harb (dziko lomwe sayendera malamulo a Chisilamu) akamva kuti ndi nthawi ya Ramadhan ndi farz kusala. 5– Kukhala muqim (okhazikika, mwachitsanzo, kuti siuli paulendo wautali.)

6- Kwa mkazi kapena mtsikana, osakhala mu nsambo (kumwezi). 7–Kwa mkazi, osakhala mu nthawi nifas.

Pali zinthu zisanu ndi chimodzi (6) zomwe zingawononge Kusala: Kudya chakudya; kumwa chakumwa; haid (nsambo); nifas (kwa mkazi amene wangobereka kumene); kusanza zinthu zodzaza mkamwa. Kunama, miseche, namima komwe ndikunena zabodza pakati pa Asilamu, ndi kulumbilira za bodza sizili m'gulu la zinthu zowononga kusala. Koma kuchita zimenezi kudzachotsa thawab imene munthu angayipeze posala kudya.

Anthu asanu ndi awiri (7) oyenera kusiya kusala kudya:

1– Munthu yemwe mutu wake siugwira; 2- Yemwe akhale Musafir pa tsiku lotsatira; (Musafir ndi munthu amene akuyenda ulendo wautali wotchedwa safar. Amatchedwanso munthu wa safari poyerekeza munthu wa muqim yemwe watchulidwa kale.) 3- Haid (Mkazi amene akudwala kumwezi); 4- Mkazi amene ali mu Nifas (nthawi yake yongotsiriza kuereka); 5- Mayi woyembekezera ngati ali wofooka kwambiri moti sangathe kusala; 6- Mkazi pa nthawi yoyamwitsa, ngati kusala kudya kungapereke chiopsyezo kwa mwana; 7- Pir-i-fani (munthu amene wakalamba kwambiri ndi wofooka kwambiri moti sangathe kusala).

Ndikofunikira kuchita niyyah (cholinga) yosala tsiku lirilonse. Kwalembedwa mu **Fatawa-i-Hindiyya** kuti: “Niyyah imachitika mu mtima. Kudzuka ndi kudya chakudya m’bandakucha chotchedwa **Sahur** kumatanthauza kuchita niyyah."

Pali mitundi iwiri ya niyyah ya kusala:

Mtundu woyamba ndi niyyah ya tsiku ndi tsiku m’mwezi wa Ramadhan, kapena kusala komwe kuli nafila (kowonjezera) kapena kusala komwe kumachitika pofuna kukwaniritsa lonjezo lina lake, niyyah yomwe iyenera kuchitika pakati pa kulowa kwa dzuwa pa tsiku lapitalo ndi nthawi ya **dahwa-i-kubra** ya tsikulo losalalo. Dahwa-i-kubra ndi theka la nthawi ya masana ya shar’i, kutanthauza theka la

nthawi ya tsiku la kusala kudya, yomwe imawerengedwa motere malinga ndi nthawi ya azani:

$$\text{Fajr} + \frac{24 - \text{Fajr}}{2} \text{ Or Fajr} + 12 - \frac{\text{Fajr}}{2} = 12 + \frac{\text{Fajr}}{2}$$

Izi zikutanthauza kuti nthawi ya dahwa-i-kubra ndi theka la chiwerengero chosonyeza nthawi ya fajr malinga ndi nthawi ya azani. Ndiye kuti isanakwane zawal (pakati pa tsiku) kutalika kwake ndi kusiyana kwa pakati pa theka la masana a shar'i ndi masana a dzuwa malinga ndi nthawi yokhazikika; kusiyana kumeneko ndikofanana ndi theka la hissa-i-fajr, yomwenso ndi nthawi yapakati pa kutuluka kwa dzuwa ndi fajr, kapena nthawi ya imsak. Mumasala pochita niyyah ngakhale mochedwa mpaka nthawi ya **Dahwai-kubra,** ngati simunadye kapena kumwa chirichonse itatha nthawi ya imsak. Nkosaloledwa kuchita niyyah pa nthawi ya Dahw. Niyyah yochita Fajr isanakwane ikhale motere: "Ndikuchita niyyah kuti mawa ndisala," pamene niyyah yochita pambuyo pa Fajr ikhale: "Ndikuchita niyyah kuti ndisala lero."

Mtundu wachiwiri wa niyyah ndi qada kapena **kaffarat** kapena **nazr-i-mutlaq**. Kusala kwa mitundu itatu iyi kumafuna niyyah ya mtundu wachiwiri. Nthawi yake yoyambilira kuchita niyyah ndi kulowa kwa dzuwa kwa tsiku lapitalo, ndipo nthawi yake yomalizira ndi kukwana kwa fajr-i-sadiq, kusanawonekere kuyera m'chizimezime. Niyyah yochita m'bandakucha utatha ndi yosaloledwa pa kusala kwa mitundu itatu iyi.

Zalembedwa m'bukhu la Ibni Abidin, kumapeto kwa mutu womwe ukufotokoza za Namaz ya qada kuti, pamene mukuchita qada ya masiku angapo osala omwe mudalephera kuchita m'mwezi wa Ramadhan wa chaka cham'buyo, simuyenera kutchula masiku omwe mukusala powatchula mayina awo kapena ndondomeko ya masikuwo. Kusala kudya kuli magawo atatu, malingana ndi anthu amene akusala kudya:

Kusala kudya kwa anthu osaphunzira; kusala kudya kwa anthu ophunzira; ndi kusala kudya kwa Anbiya (Atumiki) ndi Awliya (anthu odala omwe amapeza chikondi cha Allahu ta'âlâ). Pomwe anthu osaphunzira akusala kudya, samadya chakudya kapena kumwa chakumwa kapena kugonana. Koma amachita zolakwika zina.

Anthu ophunzira sachita zinthu zina zolakwika. Ma Enbiya ndi Awliya amapewa zokayikitsa za mtundu uliwonse pamene akusala.

Pali mitundu itatu ya Eid, kutengera anthu amene amakondwelera akamaliza kusala kudya: ‘Eid ya anthu osaphunzira; Eid ya anthu ophunzira; ndi Eid ya Anbiya ndi Awliya. Anthu osaphunzira amamasula kusala kwawo ndikudya chakudya cha madzulo, chotchedwa iftar. Iwo amadya ndi kumwa chirichonse chimene afuna, nati: “Iyi ndi Eid yathu.” Anthu ophunzira nawonso amakhala ndi iftar madzulo, koma amati: "Ndi Eid yathu ngati Allahu adhim-ush-shan wasangalala ndi kusala kwathu." Ndipo amalingalira mwakuya: “Zidzakhala bwanji kwa ife ngati IYE sanasangalale ndi ntchito zathu?”

Eid ya Anbiya ndi Awliya imakhala ru’yatullah. Akuyenera kolandira chisomo cha Allahu adhim-ush-shan.

Pali mitundu isanu ya Eid kwa okhulupilira onse:

Yoyamba: Pamene mngelo okhala ku manzere kwa Wokhulupilira sakupeze kalikonse mu dzina la ntchito zoyipa.

Yachiwiri: Pamene okhulupirira ali m’masautso a imfa (Sakaratul-mawt), angelo a nkhani yabwino amadza kwa iye ndikumupatsa moni ndi kumuwuza nkhani yabwino yakuti iye ndi wokhulupilira ndipo ndi wopita ku Mparadiso.

Yachitatu: Pamene wokhulupilira walowa mmanda mwake ndikupeza kuti ali mmunda umodzi mwa minda ya ku Mparadiso.

Yachinayi: Pamene wokhulupilira adzapezeka atakhala pamodzi ndi Anbiya ndi Awliya ndi Ulama ndi Sulaha mu nthunzi pansi pa Arsh-ur-Rahman pa tsiku la Qiyaamah.

Yachisanu: Pamene wokhulupilira wayankha mafunso onse amene adzafunsidwe m’malo asanu ndi awiri (7) pa ulendo wake wonse wa pa mulatho (ulalo) wotchedwa ‘Sirat’. Mulato umenewu ndi waung’ono kuposa tsitsi, wakuthwa kuposa lezala, ndi wakuda kuposa mdima wa usiku. Mulato umenewu ndi njira ya ulendo wa zaka chikwi kutsika phiri, zaka chikwi kukwera phiri, ndi zaka chikwi pa tyatyatya. Ngati munthu atalephera kuyankha mafunso, adzazunzidwa kwa zaka chikwi pa kulephera kulikonse. Pa mafunso asanu ndi awiriwo, loyamba lidzakhala pa Iman, la chiwiri pa Namaz, la chitatu lidzakhala pa kusala, la chinayi lidzakhala la Haji, la chisanu lidzakhala la zakat, la chisanu ndi chimodzi lidzakhala la la ufulu wa zolengedwa, ndipo la chisanu ndi chiwiri lidzakhala pa ghusl, Istinja ndi udhu. (Istinja imatanthawuza kuyeretsa kutsogolo kapena kumbuyo munthu atakodza kapena kuchita chimbudzi.)

Ngati munthu amasula mwadala (dzuwa lisanalowe) kusala kwake komwe anachita niyyah nthawi ya imsak isanakwane kudzayenera

kupepesedwa ndi kuchita qada. Kumasula kusala kowonjezera kapena kusala kwa qada sikufunika chipepeso.

Pochita kaffarat (kupepesa), kapolo amamasulidwa. Munthu amene sangakwanitse kuchita kaffarat ayenera kusala kudya masiku makumi asanu ndi limodzi (60) otsatizana. Masikuwa asakhale mkati mwa masiku a Ramadhan komanso asakhale mwa masiku asanu (5) omwe ali haram kusala. [Masiku a haram kusala ndi awa: tsiku la Eid ya Ramadhan –Eid al Fithr; tsiku la Eid-al-Adha (Eid ya Qurban); masiku atatu otsatira tsiku la Eid-al-Adha] Adzayeneranso kubwezeretsa masiku onse omwe anamasula mwadala. Munthu amene sangakwanitse kusala masiku makumi asanu ndi limodzi (60)wo, ayenera kudyetsa osauka makumi asanu ndi limodzi (60) kawiri pa tsiku kwa tsiku limodzi, kapena kudyetsa wosauka mmodzi kawiri pa tsiku kwa masiku makumi asanu ndi limodzi (60). Kapena amapereka Chuma kwa aliyense (mwa anthu 60 aja) chomwe kuchuluka kwake ndi kofanana ndi zomwe zikuperekedwa monga Fitra.

Kuchita qada ya kusala kudya kwa tsiku limodzi, mumasala tsiku limodzi.

Anthu asanu safunika kuchita kaffarat (kupepesa). Woyamba ndi munthu wodwala. Wachiwiri ndi musafir, (amene ali pa ulendo wautali wotchedwa safar.) Wachitatu ndi mayi woyamwitsa ndipo sanasale kuwopera kuti mwana angakhale pa chiopsyezo. Wachinayi ndi pir-i-fani (wokalamba). Wachisanu ndi munthu amene akhoza kufa chifukwa cha njala kapena ludzu.

Pomwe udhr (chowalola kusasala) chawo chatha anthu amenewa adzayenera kuchita qada tsiku limodzi kwa tsiku limodzi.

Pali mitundu ingapo ya niyyah ya **yawm-i-shakk**,[1]: Pa yawm-i-shakk (tsiku lokayikitsa) ndi kololedwa, ngakhale ndi karahat (zosalamulidwa), kuchita niyyah ya kusala tsiku limodzi mu Ramadhan kapena kwa tsiku lina lomwe liri wajib kapena kuchita niyyah yosala tsiku limodzi mu Ramadhan, ngati ndi Ramadhan, kapena kusala komwe kuli nafila (kowonjezera) kapena komwe si wajib, ngati tsikulo si tsiku Ramadhan. Mtundu wina wa niyyah ndi yomwe ilibe karahat ndipo imachitika kusala kudya wamba kapena kusala mu Sha'ban, komwe ndi kuchita niyyah ya kusala kwa nafila. (Karahat ndi chinthu monga machitidwe, nthawi zomwe sizabwino kapena zimene Mtumiki

[1] Kutanthauza tsiku lokayikitsa, pa Chiyankhulo. Pa Chisilamu, zimatanthauza tsiku lomwe silidziwika kuti ndi tsiku loyamba la Ramadhan kapena tsiku lomaliza la Sha'ban.

wathu “sallallâhu alaihi wa sallam” sanalangiza kuti zichitike ngati ntchito zopembedza. Ngati ntchitoyo ili yowonjezera, isachitike mkati mwa nthawi ya karahat. Ngati ntchito yakupembedza ili fardh ndipo simunachite, ngakhale inayenera kuchitika nthawi yake yoyikidwa isanathe, muyenera kuchita ungakhale mutachita mu karahat.

Mtundu wa kusala omwe siwololedwa ndi umene niyyah yake ili motere “Ndikuchita niyyah yosala ngati mwezi wa Ramadhan wawoneka; ngati si unawoneke ndiye kuti sindinachite niyyah.”

Tiyerekeze kuti munthu sanachite Niyyah mpaka kutha kwa Fajr, mpaka kumbali yakummawa kukuwonekera kuyera mu Ramadhan. Ndi kudya chinthu masanaasanakwane; munthu uyu sakuyenera kuchita kaffarat, kapena kuti kusala masiku makumi asanu ndi limodzi (60) motsatizana Ramadhan ikadzatha. Izi ziri chonchi malinga ndi Imam Azam Abu Hanifa. Koma malinga ndi Imamayn, munthu uyu amayenera kuchita kaffarat, chifukwa wadya pomwe kunali kotheka kwa iye kuchita Niyyah ndi kusala kudya kwake. Ngati atadya dzuwa litapendeka, sakuyenera kuchita kaffarat, - molingana ndi ijtihad yomwe onse anavomerezana.

Ngati munthu waphwanya kusala kwake miyezi iwiri kapena itatu m’miyezi ya Ramadhan, pa kudya nthawi yake isanakwane kamodzi m’mwezi uliwonse wodalitsika, kodi akuyenera kuchita kaffarat pa kuphwanya kulikonse padera-padera, kapena ndi kokwanira kuchita kaffarat kamodzi pa kuphwanya ku wiri kapena ku tatuko? Pali kutsutsana pa nkhaniyi pakati pa a katswiri a Chisilamu. Kungakhale kwanzeru kuchita kaffarat padera padera pa kuphwanya kulikonse. Tiyerekeze kuti munthu ali ndi ngongole ya kusala kudya m’Ramadhan; malinga ndi kunena kwa akatswiri ena, munthu ameneyo amakhala wotchimwa ngati chaka chimodzi chadutsa ndipo munthuyo sanalipire ngongole yake posala kudya tsiku kapena masiku omwe ali nawo ngongole yakusala.

Tiyerekeze kuti nthawi ya Eid imodzi mwa ma Eid awiri a pa chaka omwe ndi Eid ya Ramadhan-i-Sharif kapena Eid ya Qur'ban, yafika munthu akuchita kaffarat. Ndi zachidziwikire kuti ndi haram kusala kudya pa masiku a Eid, ngakhale atasala pa chifukwa chotani. Iye ayenera kumasula ndi kudzayambiranso kusala kudya kwa kaffarat kuyambira pachiyambi (masiku onse 60). Masiku omwe anasala poyamba sadzawerengedwanso pokwaniritsa kusala kwa masiku makumi asanu ndi limodzi (60).

Ngati munthu wamasula kusala kwake popanda kuchita niyyah yake ya ulendo wautali, kenako ndikuchita niyyah yake ya safar ndi

kunyamuka, adzayenera kuchita kaffarat ndi qada yomwe, (adzayenera kubwezeretsa kusala kudya tsiku limodzilo ndi masiku makumi asanu ndi limodzi (60) otsatizana pa chilango chotchedwa kaffarat.) Kuyenda ulendo wautali si chinthu chochititsa mubah (chololedza) kumasula kusala. Munthu akayenda ulendo wautali (Safar), zili wajib kwa iye kuti asamasule tsiku limenelo.

Ngati Musafir (munthu wa pa ulendo wautali) achita niyyah yake ya kusala usiku kapena nthawi ina iliyonse isanakwane nthawi yotchedwa Dahwa-i-kubra, sizili halal kwa iye kusiya kusala tsiku limenelo. Ngati akumasula kusala kwake, adzayenera kubweza tsiku lomwe wamasulalo, (adzasala tsiku limodzi pambuyo pa mwezi wodalitsika wa Ramadhan). Chomwe chimachititsa ulendo wautali kukhala mubah ndi: 'Kusayamba kusala kwa tsiku ndi tsiku'.

Munthu amene mutu wake usakugwira ntchito bwino nthawi ya Ramadhan, moti sangasale chakudya, kenako ndi kudzachira, adzachita qada masiku omwe analephera kusalawo. Ngati sakuchira mu Ramadhan yonse, moti vuto lake la m'maganizo likupitilirabe, ndiye kuti wamasulidwa ku kusala kudya kwa Ramadhan. Iye sangawerengedwe kukhala mgulu la anthu osala.

Munthu akayiwala kuti wasala ndipo wadya, kusala kwake sikukhala fasid (sikungawonongeke). Akakumbukira kuti wasala koma ndi kupitiriza kudya chifukwa akuganiza kuti kusala kwake kuli fasid (kwawonongeka), ndiye kuti wamasuladi. Adzachita qada Ramadhan itatha, ndipo sadzachita kaffarat. Koma akapitiriza kudya ngakhale akudziwa kuti kusala kwake sikuli fasid, ndiye kuti wachita akudziwa, adzafunika kuchita qada ndi kaffarat yomwe.

Munthu yemwe wasala kudya akameza thukuta lake kapena kutafuna chingwe chopakidwa utoto kenaka ndi kumeza utotowo, kapena kumeza malovu a munthu wina kapena kumeza malovu ake atawasunga m'kamwa mwake dala, kapena kumeza chakudya chotsalira pakati pa mano ake chomwe ndi chokulirapo ngati nandolo, kapena kudzibaya mankhwala ndi jakisoni, kusala kwake kumawonongeka ndipo adzangochita qada yopanda kaffarat.

Ngati munthu wadya pepala kapena mchere wodzaza dzanja kapena kumeza njere ya tirigu kapena mpunga, kusala kwakeko kumawonongeka. Koma adzangochita qada popanda kaffarat. Poti si mwambo kudya mchere wodzaza dzanja ngati chakudya kapena mankhwala. Zili ngati dothi lodzadza dzanja. Koma ngati mchere womwe wadya ndi wapang'ono, ndiye kuti kaffarat idzachitika. Izi

zalembedwa m'bukhu lotchedwa **Eshbah.** Poti mchere wapang'ono umagwiritsidwa ntchito ngati chakudya komanso mankhwala.

Ngati wantchito akudziwa kuti adzadwala pogwira ntchito yozipezera zofunika pa moyo wake, nkosaloledwa kwa iye kusiya kusala asanadwale. Ngati amasula kusala kwake nthawi ya Ifar isanakwane, adzafunika kuchia kaffarat. Kuti apewe kuchita kaffarat, ayambe kumeza kapepala asanadye chirichonse. Ngati mzimayi wapakati kapena yemwe akuyamwitsa akumva kufowoka kwambiri ndi njala, ludzu, ndi zina zotero kuti sangapitirire ndi kusala kwake, ndipo wadya kapena kumwa, adzangochita qada. Munthu amene amadya ndi kumwa monyozera ndi mopanda udhr (chifukwa chomuyenereza) kutero masana mu Ramadhan, amakhala murtadd (wopatuka). (Fatawa-iFayziyya.)

Munthu akatafuna njere ya chitowe, kusala kwake sikukhala fasid. Koma akameza, kaya watafuna kapena ayi, kusala kwake kumakhala kopanda phindu. Kudzafunika kuchita qada yake.

Kusala kulipo mitundu khumi ndi isanu: mitundu itatu mwa iyo ndi farz, itatu mwa iyo ndi wajib, isanu mwa iyo ndi haram, inayi ndi sunnat. Kusala kudya kutatu (3) komwe kuli farz ndi: kusala m'mwezi wa Ramadhan, kusala kochita qada, ndi kusala kwa kaffarat.

Kusala kudya kutatu (3) komwe kuli wajib ndi: Kusala kwa nazr-i-mu'ayyan, kusala nazr-i-mutlaq, ndi kusala kwa nafila mpaka kulowa kwa dzuwa ukangoyamba kuchita.

Kusala kudya kusanu (5) komwe kuli Haramu ndi: Kusala kudya pa tsiku loyamba a Eid-al-Fithr, kusala kudya pa Eid-al –Adha (Eid ya Qurban) ndi kusala chakudya tsiku lililonse mwa masiku atatu otsatira Eid ya Qurban. Ndi haram kusala tsiku lirilonse mwa masiku asanu amenewa.

Kusala kudya kunayi komwe kuli sunnat ndi: Kusala kudya pa **ayam-i-baydhi** m'mwezi uliwonse (wa Chiarabu). Kusala masiku otchedwa sawm-i-Dawud; kusala lolemba ndi la chinayi; kusala tsiku la Ashura; kusala tsiku la Arafa, ndi kusala pa masiku odalitsika ofanana. Tsiku la khumi ndi chinayi (14), khumi ndi chisanu (15) ndi khumi ndi chisanu ndi limodzi (16) a mwezi wa Chiarabu amatchedwa **ayyam-i-baydhi**. Kusala kudya tsiku lina lirilonse modumpitsa tsiku limodzi lirilonse chaka ndi chaka, kumatchedwa **sawm-i-Dawud. Tsiku la Ashura** ndi tsiku la khumi (10) mwezi wa Muharram, mwezi woyamba wa Chiarabu. **Tsiku la Arafa** ndi tsiku la chisanu ndi chinayi (9) la mwezi wa Chiarabu wa **Du'l-hijja**, tsiku lomwe mmawa wake ndi tsiku loyamba la Eid ya Qurban.

Pali maphindu khumi ndi limodzi pa kusala kudya:

1- Kusala kumamuchinga munthu ku Jahannama.

2- Kusala kumachititsa kuti mapemphero ena omwe munthu wachita avomerezedwe ndi Allahu ta'âlâ.

3- Kusala ndi dhikr yochitidwa ndi thupi la munthu. (Dhikr ndi njira yotamandira Allah ta'âlâ.)

4- Kusal kumachotsa kibr mwa munthu. (Kibr ndi khalidwe monga kudzitama, kudzimva, zopanda pake).

5- Kusala kumachotsa ujb mwa wokhulupilira (kunyada ndi kudzikuza pochita zake zopembedza).

6- Kusala kumaonjezera khushu (kuopa Allahu ta'âlâ).

7- Thawab zopeza chifukwa cha kusala zidzayikidwa pa mizan. Mizan ndi sikelo yoyezera ntchito zabwino za munthu m'moyo uli nkudza.

8- Mulungu amasangalala ndi kapolo Wake yemwe akusala.

9- Ngati munthu amwalira ali ndi Imaan, kusala kudya kwake kudzamuchititsa kulowa ku Mparadiso moyambilira.

10- Mtima wa munthu umakhala wowala ndi nuru.

11- Maganizo a munthu amawalitsidwa ndi nuru.

Dzuwa likalowa pa tsiku la makumi awiri mphambu zisanu ndi zinayi (pa 29) la mwezi wa Sha'ban, ndi wajib kuyang'ana mwezi watsopano wa Ramadhan chakumadzulo komwe kumawonekera mwezi. Msilamu amene ali adil, yemwe sachita tchimo lalikulu, ndipo ali m'Madhhab a Ahl as-sunnat, akaona mwezi watsopano kumwamba kutaphimbika ndi mitambo, amadziwitsa woweruza bwalo la milandu kapena bwanamkubwa. Ramadhan imayamba pomwe Msilamu wawona mwezi watsopano. Umboni woti mwezi wawoneka operekedwa ndi munthu yemwe ndi wa bid'ah kapena yemwe ali fasiq (munthu wopwanya malamulo a chisilamu) siumakhala ovomerezeka. Ngati nyengo iri bwino, pakufunika anthu angapo achitire umboni kuti awuona mwezi woyambira Ramadhan ndi maso awo. Ngati mwezi watsopano siuoneka, ndiye kuti mwezi wa Sha'ban wa chaka chimenecho umavomerezedwa kukhala wa masiku makumi atatu, ndipo tsiku lotsatira ndilo tsiku loyamba la mwezi wa Ramadhan. Chiyambi cha Ramadhan sichidziwika ndi kalendala kapena kuwerengera za kuthambo (pounikira makina). Kwalembedwa m'mabuku otchedwa **Bahr-ur-raiq, Fatawa-i-Hindiyya** ndi **Qadikhan** kuti: "Ngati kapolo yemwe akukhala ku **Dar-ul-harb** ndipo sakudziwa tsiku loyambira Ramadhan ndipo akugwiritsa ntchito kalendala ndi

kusala kwa mwezi umodzi, ndi zotheka kuti anayamba mofulumira ndi tsiku limodzi kapena anachedwa ndi tsiku, kapena anayambadi pa tsiku loyamba la Ramadhan. Ngati anafulumira ndi tsiku limodzi, ndiye kuti adzakondwelera Eid pa tsiku lomaliza la Ramadhan. Ngati anachedwa ndi tsiku limodzi ndiye kuti adzasala kudya pa tsiku la Eid poganiza kuti akusala kudya pa tsiku lomaliza la Ramadhan. Muli monse pamenepo ndiye kuti wasala kudya masiku makumi awiri mphambu asanu ndi atatu (28) a mwezi wa Ramadhan; choncho adzayenera kusala masiku awiri ndi cholinga cha qada Eid itachitika. Potengera gawo lachitatu, ndi zokayikitsa ngati masiku oyambira ndi omalizira a mwezi womwe anasala akugwirizana ndi Ramadhan. Popeza kusala kudya masiku okayikitsa kuti anali mkati mwa Ramadhan sikudzakhala sahih, wokhulupilirayo adzafunikanso kusala masiku awiri a qada." Choncho, anthu amene amayamba kusala kudya mu Ramadhan posatsatira kuoneka kwa mwezi watsopano kumwamba koma potsata ma kalendala omwe adakonzedwa kale, adzayenera kusala masiku awiri ndi cholinga cha qada Eid ya Ramadhan itachitika.

[Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ" akuti: "Mu nyengo ya mvula iftar isachitike (osamasula kusala) pokhapokha munthu atatsimikiza kuti dzuwa lalowa, ngakhale azan ya Mangrib yachitika."

Munthu wosala akuchita iftar nthawi yotchedwa **ishtibak-un-nujum** (nthawi yomwe nyenyezi zambiri zimaonekera kumwamba) isanakwane, Munthuyo amakhala kuti wachita mustahab yotchedwa **'ta'jil',** kutanthauza "Kufulumizitsa pochita iftar". Dzuwa likalowa ndipo iftar ikuchitika pamalo ena ake, munthu yemwe ali pamalo okwera, mwachitsanzo amene ali pa minaret, sayenera kuchita iftar pokhapokha atawona kuchokera pomwe iye ali kuti dzuwa lalowadi. Lamuloli likugwiranso ntchito pa mapemphero a m'mawa ndi sahur (dakwi)." Mu m'ndandanda wa **Tamkin** m'mabuku a Astronomy, kutalika kochokera pansi kupita mmwamba ndi chimodzi mwa zomwe zimachititsa kusiyana kwa nthawi komwe kumatchedwa tamkin**.** Monga momwe nthawi zonse za mapemphero zimawerengetsedwera, nthawi imodzi ya tamkin imagwiritsidwa ntchito pa malo ake-ake. Mwachitsanzo, nthawi ya tamkin ya malo okwera ikhoza kusiyana pang'ono ndi malo otsika. Kalendala zokonzedwa popanda kuganizira nthawi za tamkin zimapereka nthawi za kulowa kwa dzuwa mofulumira ndi mphindi zingapo kusiyana ndi nthawi za kulowa ka dzuŵa zomwe zawerengedwa poganizira nthawi za tamkin). Dzuwa silimaoneka kuti lalowa pa nthaŵi yolowa yolembedwa pa ma

kalendala amenewo. Kusala kochitidwa ndi anthu omwe amachita iftar molingana ndi makalendala opanda tamkin amakhala fasid.]

NSEMBE (QURBAN)

Pali zofunika zitatu zoti zikwaniritsidwe kuti nsembe (Qurban) iperekedwe:

1. Opereka akhale Msilamu wozindikira ndi wotha msinkhu.

2. Opereka akhale muqim (okhazikika, kutanthauza kuti asakhale safari).

3. Opereka akhale ndi chuma chokwanira nisab (mulingo wa nsembe).

Rukn (nsichi yofunikira) kuti nyama iphedwe ngati nsembe (Qurban); kaya nkhosa, mbuzi, kapena ng'ombe ya mphongo kapena ngamira, zimakwanira ma qurban asanu ndi awiri, kutanthauza kuti anthu asanu ndi awiri atha kupha ng'ombe (imodzi) ngati qurban kwa onse asanu ndi awiri. Ngati wina anena kuti, "Ndiloleni kuti ndiphatikizidwe nawo," qurban ya munthu wachisanu ndi chitatuyo imakhala fasid (yopanda pake). Nisab ya Qurban ndi yofanana ndi nisab ya Fitra.

[Monga zanenedwera ndi Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ" kuti ngati gawo la aliyense wa iwo likhala lochepera pa gawo limodzi mwa magawo asanu ndi awiri, palibe qurban idzaloledwa mwa anthu asanu ndi awiriwo. Choncho, nkololedwa kwa anthu osakwana asanu ndi awiri kusonkherana Qurban pamodzi. Ndi sahih (zovomerezeka) kutenga nawo mbali pa nthawi yogula. Ngakhale ndi sahih kutenga nawo gawo mutagula, ndi bwino kutenga nawo mbali musanagule. Munthu atha kuchita Qurban mogwirizana ndi munthu wina pogula kuchokera gawo limodzi mwa magawo asanu ndi awiri mpaka asanu ndi limodzi mwa magawo asanu ndi awiri a ng'ombe yayimuna (kapena ng'ombe yayikazi) yomwe ali nayo winayo. Amagawana nyama molingana ndi magawo a momwe anasonkhera. Ngati mmodzi mwa osonkherana naye amwalira, zidzakhala sahih ngati mlowam'malo wake atanena (kwa anzakewo): "Mchitireni Qurban m'malo mwake ndi mmalo mwa inu nokha." Ndithu, ndi ntchito ya Qurbat kuchita Qurban m'malo mwa Msilamu wakufa. Ngati olowa mmalo sanena choncho, Qurban ya omwalirayo siidzakhala Qurban ndipo palibe qurban za osonkherana nawo yomwe idzakhale Sahih. Ngati mmodzi mwa ophatikizana naye ali kafiri, kapena ngati analowa

m’chiyanjanocho chifukwa cha nyama, palibe Qurban yomwe idzaloledwa.

Pakuti, aliyense pa gulupo ayenera kuchita niyyah ya Qurbat. Niyyah ya wosakhulupilira ndi batil (yopanda pake). Kuchita niyyah kuti adye, si ntchito ya Qurbat. Chimodzimodzi ngati mmodzi mwa ophatikizanawo achita Niyyah ya Qurban ya chaka chino, ndipo enawo achita Niyyah ya Qurban ya chaka chammawa, niyyah ya enawo ndi batil (yachabechabe) ndipo nyama ya m'magawo awo imakhala tatawwu [chopereka chabe], ndipo ayenera kugawa ngati mphatso ya chifundo kwa osauka. Niyyah yopangidwa ndi woyambayo ndi sahih (yovomerezeka), koma kenako sangadye nyamayo. Pakuti, chiweruzo choti nyama iyenera kuperekedwa monga mphatso za chifundo chafalikira mu nyama yonse. Niyyah ya qurbat (kuziyandikisa) yomwe yapangidwa sikuyenera kukhala qurbat yomwe ili wajib. Itha kukhalanso qurbat yomwe ndi Sunnah kapena nafila. Ikhozanso kukhala qurbat yomwe ili ndi machitidwe osiyanasiyana a wajib. Ndi zololedwanso kuti itha kukhala Aqiqa kwa mwana kapena wamkulu. Pakuti, 'Aqiqa ndi (qurbat) Kuziyandikisa kochitidwa ngati nsembe yothokoza chifukwa chodalitsidwa ndi mwana wakhanda. Komanso, kusonkhana kwa Asilamu pa chakudya chosangalalira kuchitika kwa nikah, ndi mtundu wa chiyamiko ndi qurbat yomwe ili Sunnah. Chofunikira kwambiri ndi choti onse ogwirizana achite niyyah yawo ya Qurban ya Eid. Kupha nyama chifukwa cha 'Aqiqa si ntchito ya Sunnah m’Madhhab a Hanafi. Ndi mustahab kapena mubah.

Ntchito ya mustahab ndi Qurbat. Nayonso ntchito ya mubah ndi qurbat ikachitika ndi Niyyah yothokoza. Palinso miyambo ina yambiri yomwe imakhala ntchito zopembedza malinga ndi niyyah yomwe yachitika. Mubah imasandukanso ntchito ya ta’at munthu akachita niyyah (ya ta’at). Mabuku a Chiarabu otchedwa **Uqud-ud-durriyya** ndi **Durr-ulmukhtar** amafotokoza mwatsatanetsatane zakupha (kuzinga) nyama ya Aqiqa.]

HAJI
(ULENDO WOPITA KU MZINDA WOPATULIKA WA MAKKA)

Haji ili ndi rukn (nsichi) zitatu:

1– Kuchita niyyah ya Haji povala chovala chapadera chotchedwa **ihram**.

2- Kuchita waqfa pa phiri la Arafat.

3- Kuchita Tawaf ziyarat pa Ka’ba.

Nthawi yolawirira yochitira waqfa pa Arafat ndi pakati pa nthawi ya zawal (dzuwa liri pa liwombo) pa tsiku la chisanu ndi chinayi m'mwezi wa Dhu'lhijja ndi m'mawa wotsatira. [Ngati mukuyima waqfa tsiku limodzi mofulumira kapena mochedyera, Haji imene mukuchita imakhala batil (yopanda pake). Ma Wahhabis amakondwelera Eid (ya Qurban) tsiku limodzi mofulumira. Haji yochitidwa ndi anthu amene sayima waqfa mkati mwa nthawi yoyikika, motero si sahih (siyovomerezeka).]

Pali mitundu isanu ndi iwiri ya tawaf (kuzungulira Ka'ba mu'azzama mkati mwa Masjid-i-haram):

Woyamba ndi tawaf ziyarat.

Wachiwiri ndi tawaf ya umra.

(Mitundu iwiri ya tawaf iyi ndi fardh.)

Wachitatu ndi tawaf qudum, yomwe ndi Sunnah.

Wachinayi ndi tawaf ya wada (yotsanzika).

Wachisanu ndi tawaf ya nazr, yomwe ndi wajib.

Wachisanu ndi chimodzi ndi tawaf nafila.

Wachisanu ndi chiwiri ndi tawaf ya tatawwu, yomwe ndi mustahab.

Ndi fardh kuchita niyyah povala ihram ya Haji. Ndi Sunnah kuvala chidutswa chansalu yotchedwa ihram. Ndi wajib kupewa kuvala zovala zosokedwa.

Pali zinthu zisanu ndi zitatu zomwe ziyenera kukwaniritsidwa kuti zikhale fardh kwa munthu wochita Haji.

1- Kukhala Msilamu.

2- Kukhala wakutha msinkhu.

3- Kukwana zaka zozindikira.

4- Kukhala wathanzi.

5- Asakhale kapolo.

6- Kukhala ndi katundu woposa zofunika za munthu.

7- Ikhale nthawi ya Haji. Nthawi ya Haji ndi tsiku la Arafa ndi masiku anayi Eid (ya Qurban). Masiku omwe amakhala oyenda popita amawonjezeredwa powerengera.

8- Kwa mkazi wa kutali ndi Makka oti adzayenda mtunda wawutali (ulendo wautali wotchedwa) safar, ulendo wa masiku atatu, kapena ulendo wa makilomita zana limodzi ndi anayi, malinga ndi Madhhab a Hanafi, ayenera kutsagana ndi mamuna wake kapena ndi wachibale

wake wa mamuna yemwe ndi Mahram kwa iye (amene iye saloledwa kupangana naye ukwati wa Chisilamu wotchedwa nikah). [Ndi fardh kwa anthu amene akwaniritsa zoyenerezazi zisanu ndi zitatuzi kuchita Haji kamodzi pa moyo wawo wonse. Ngati achita haji kangapo, ndiye kuti Haji yomwe amakachita mzaka zotsatirazo ndi nafila. **Kupembedza komwe ndi nafila** ndi komwe wachita mwakufuna kwake ngakhale si fardh kapena Sunnah (kuchita). Thawab yopembedza nafila, poiyerekeza ndi thawab yopembedza fardh, ndi yocheperapo ngati dontho la madzi poyerekeza ndi madzi a m'nyanja.

Akadaulo amaphunziro a Chisilamu sanavomereza kuti Asilamu okhala kumadera akutali ndi Makka akachite Haji kachiwiri. Abdullah-i-Dahlawi quddisa sirruh akunena motere mu Kalata ya makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu zitatu (63) m'bukhu lake lofunika kwambiri lotchedwa **Mekatib-isherifa**: "Pa ulendo wokachita Haji, kumakhala kosatheka kuchita zopembedza moyenera. Pa chifukwa chimenechi, Imam Rabbani “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih” akunena m'makalata ake 123 ndi 124 m'bukhu loyamba la ntchito yake yodalitsika yotchedwa Maktubat kuti sakugwirizana nazo zopita pa ulendo ndi cholinga chokachita ‘Umra kapena haji ya nafila.”[1] Nafila Haji ndi haram ngati ikulepheretsa kupembedza komwe ungathe kupewa nako haram kapena kulepheretsa mkazi kuvala chovala chake moyenera. Kupita ku nafila Haji ya mtundu uwu kumabweretsa utchimo, mmalo mopezetsa thawab. Zirinso chimodzimodzi kupita paulendo wokachita Umra.

MA FARDH 54
(MA UDINDO ACHPEMBEZO OLAMULIDWA NDI ALLAH -54)

Mwana amakhala **Msilamu** akatha msinkhu. Munthu amene sali Msilamu amakhala Msilamu akachita **Kalima tawhid**, kunena kuti, **“La illaha illallah Muhammadun rasulullah,”** ndi kukhulupilira Tanthauzo la zomwe zanenedwa. Machimo onse amene anachita asanakhale Msilamu amakhululukidwa pomwepo ndi Allahu ta’âlâ. Koma anthu awiriwa, monga Msilamu wina aliyense, ayenera kuloweza pa mtima nsichi zisanu ndi imodzi za iman, zomwe pamodzi zimatchedwa **Amentu**. Akapeza nthawi, aphunzire matanthauzo ake ndi kuwakhulupirira, ndi kunena, "Ndikukhulupiira muchowonadi kuti

[1] Makalata awiriwa analembedwa kwa Molla Tahir Bedakhshi. Zomasulira zachingerezi za kalatazi ndi mbiri mwachidule ya Tahir Bedakhshi zomwe zawonjezedwa ku buku la-makono.

Chisilamu chonse, malamulo onse ndi zoletsedwa zonse mophatikiza pamodzi, zalengezedwa ndi **Allahu ta'âlâ**. Kenako akakhala ndi nthawi kapena mpata wabwino, zimakhalanso fardh kwa iwo kuphunzira zinthu zomwe ziri za Fardh, zinthu zomwe walamulidwa ndi zinthu zomwe ziri haram, zoletsedwa muziphunzitso zonse za Chisilamu zokhudzana ndi chikhalidwe ndi zochitika zatsopano zomwe iwo angakumane nazo zotsutsana ndi zomwe amachita. Ngati akanira kapena osakhulupilira, kapena kunyozera mfundo yakuti ndi fardh kuphunzira izi, ndi kuti ndi fardh kuchita zomwe ziri za Fardh ndi kupewa chilichonse mwa zomwe zili haram, ndiye kuti asanduka **murtadd** (wampatuko). M'mawu ena, munthu amene amanyoza chimodzi mwa ziphunzitso zimenezi, mwachitsanzo, kudziphimba kwa akazi (momwe Chisilamu chimalamulira) amakhala murtadd.

Pokhapokha ngati murtadd atachita tawba chifukwa cha kupatuka kwakwe, sadzakhala Msilamu ponena kuti, **"La illaha illallah"** kapena pochita ena mwa malamulo a Chisilamu, monga kuchita Swalah, kusala kudya, kupita ku Haji kapena kuchita zabwino ngati kepereka sadaka, ndipo sadzapeza phindu pa ntchito zake zabwinozi pa tsiku lomaliza. Ayenera kulapa ndi kuchita tawba chifukwa chokanira, nsichi ya Chisilamu yomwe wakana kuyikhulupilirayo."

Akatswiri a Chisilamu asonkhanitsa fardh 54 zomwe Msilamu aliyense ayenera kuzikhulupilira ndi kuzitsatira:

1- Kudziwa kuti Allahu ta'âlâ ndi Mmodzi, ndipo osamuyiwala.

2. Kudya ndi kumwa za halal

3- Kuchita udhu

4- Kuchita Swalah zisanu tsiku lirilonse ikafika nthawi yake.

5- Pomwe mukufuna kuchita Swalah chitani ghusl ya haid (ngati ndi mtsikana kapena mkazi) ndi ya Junub

6- Kudziwa motsimikiza ndi kukhulupilira kuti Allahu ta'âlâ amakonzeratu rizq (zakudya) za munthu.

7- Kuvala zovala za ukhondo ndi za halal.

8- Kugwira ntchito ndi kuyika tawakkul (kudalira) kwako mwa Allahu ta'âlâ.

9- Kukhala wokhutira.

10- Kunena mawu othokhoza kwa Allahu ta'âlâ chifukwa cha mphatso Zake. Kugwiritsa ntchito mphatso zochokera kwa Allah ta'âlâ pa malo oyenera ndi m'njira zomwe zinalamulidwa.

11- Kulandira qada (malamulo) omwe akuchokera ku Janab bari mogonjera.

12- Kukhala woleza mtima pa zochitika zadzidzidzi. Ndiko kuti, osazitsutsa.

13- Kuchita tawba chifukwa cha machimo (ochitika). Kuchita pemphero lotchedwa istighfar tsiku lirilonse.

14- Kuchita mapemphero mwa ikhlas. (Ndiko kuti, kupembedza chifukwa cha chisomo cha Allahu ta'âlâ chokha, ndi cholinga chomukondweretsa Allahu subhanahu wa ta'âlâta'âlâ.)

15- Kuwawona a satana a mwa anthu ndi ziwanda ngati adani ako.

16- Kukhala ndi Qur'an adhim-ush- ndi kuyitenga ngati malemba a chitsimikizo. Ndikugonjera ku zigamulo zake.

17- Kudziwa kuti imfa ndi Haqq (Chifuniro cha Allahu ta'âlâ), ndi kukonzekera imfa.

18- Kukonda chirichonse ndi onse amene Allahu ta'âlâ amawakonda ndi kupewa zonse (ndi amene) Allah ta'âlâ amadana nazo. [Izi zimatchedwa Hubb fillah ndi bughd fillah.]

19- Kukhala wabwino kwa makolo ako.

20- Kulimbikitsana pochita zabwino ndi kuletsana kuchita zoipa.

21- Kukayendera abale a mahram.

22- Osagwiritsa ntchito molakwika kudalirika kwa wina.

23- Kuwopa Allahu subhanahu wa ta'âlâa anthawi zonse ndi kupewa kuchita zoyipa.

24- Kumvera Allahu ta'âlâa azeem ul shan ndi Mtumiki Wake. Ndiko kuchita zinthu za fardh ndi kupewa zoyipa.

25- Kupewa kuchimwa ndi kugwiritsa ntchito nthawi yako pochita mapemphero.

26- Osanyoza ulu emr ndipo osaphwanya malamulo.

27- Kuona chilengedwe chonse chozungulira iye ndi chidwi chachikulu.

28- Kusinkhasinkha za kukhalapo kwa Allahu ta'âlâ, mbiri Zake ndi zolengedwa Zake.

29- Kuteteza lilime lako kuzoletsedwa ndi zoyankhula zolaula.

30- Kuyeretsa mtima wako pozitalikitsa ku ma-siwa [kukonda dziko lapansi].

31- Osanyogodola aliyense.

32– Kusayang'anitsitsa chinthu chomwe chiri haram.

33– Kusunga malonjezo anu ngakhale zitavuta bwanji

34– Kuteteza makutu anu kuti musamvere zinthu zoyipa monga zotukwana ndi zida zoyimbira.

35- Kuphunzira kapena kudziwa fardh ndi haram

36- Kugwiritsira ntchito miyezo ndi zida zoyezera mwachilungamo,

37– Osanyozera mavuto omwe Allahu azeem ul shan angakuninkheni nawo ndi kukhala ndi mantha nthawi zonse.

38- Kulipira zakat kwa Asilamu osauka ndi kuwathandiza.

39- Osataya chiyembekezo cha chifundo cha Allahu subhanahu wa ta'âlâ

40- Kusadzilowetsa m'zilakolako za haram zokhumba za mtima wako

41- Kumdyetsa wa njala m'chisomo cha Allahu subhanahu wa ta'âlâ

42– Kugwira ntchito ndi kupeza rizq lokwanira, [monga chakudya, zovala ndi pogona].

43- Kulipira zakat pa chuma chanu ndi "usher pa zokolola zanu."

44- Kusagonana ndi mkazi wako pa nthawi ya nsambo wake ndi panthawi yomwe sanamalize masiku ake obereka.

45- Kusunga mtima wanu woyera kuchokera ku machimo.

46- Kupewa kudzikweza

47- Kuteteza chuma cha mwana wamasiye yemwe sanakwanitse zaka zakutha nsinkhu.

48- Osakhala pafupi ndi anyamata achichepere.

49- Kuchita Swalah zisanu za pa tsiku mu nthawi yake, osachedwetsa mpaka nthawi yake yoikika itatha.

50- Kusalanda chuma cha aliyense.

[Ndi ufulu wa chibadwidwe kupereka ndalama zotchedwa mahr kwa mkazi wanu pamene mukumusudzula. Kusapereka Ufulu umenewu kumadzetsa chilango chaukali pa dziko la pansi ndi chilango chowawa pa tsiku lomaliza. Mwa ufulu wa anthu, chofunika kwambiri ndi kuchita emr ma'ruf kwa abale ako ndi kwa anthu amene ali pansi pa ulamuliro wako, (ndiko kuwaphunzitsa Chisilamu), ndipo umakhala ndi chilango chopweteka (pa tsiku lomaliza) ukanyalanyaza.

Munthu amene akuwaletsa (abale ake ndi anthu amene ali pansi pa ulamuliro wako) ndi Asilamu ena onse kuphunzira chipembedzo chawo ndi Kafiri. Yemwe angawaletse kuchita mapemphero awo

powakhaulitsa ndi mazunzo ndikuwakonzera ziwembu, nayenso ndi kafiri komanso mdani wa Chisilamu. Chitsanzo pa zimenezi ndi anthu a bidah ndi wopanda madhhabi omwe amayipitsa chikhulupiliro cha Ahl asSunnah ndi kusokeretsa Asilamu kuchokera m'Chisilamu ndi iman poyankhula ndi kusindikiza zosokoneza.

51- Osamphatikiza Allahu subhanahu wa ta'âlâ ndi zinthu zina

52- Kupewa dama.

53- Osamwa vinyo ndi zakumwa zina zoledzeretsa.

54- Osadzinyenga wekha.

[Vinyo ndi mowa ndi zakumwa zina zonse zoledzeretsa ndi qaba Najasi, Zalembedwa m'mabuku a **Bahr-ur- raiq** ndi **Ibni 'Abidin** kuti madzi ndi nthaka zikasakanizidwa pa modzi, matope otulukapo adzakhala oyera ngati chimodzi mwa zinthu ziwirizo ziri zoyera. Umboni wakuti qawl iyi ndi imodzi ya sahih, ndikoti fatwa yomaliza imagwirizana ndi ijtihad imeneyi. Ngakhale alipo akatswiri amene amanena kuti fatwa imeneyi ndi da'if (yofooka). Zinalembedwa mu '**Ibni' Abidin** ndi **Hadiqa** kuti qawl ya da'if ingagwiritsidwe ntchito pakakhala haraj (zovuta). Ichi ndi chifukwa chake zinthu zofunika zomwe zimasakanizidwa ndi mowa popanga, zimakhala zoyera. Zitsanzi ndi vanishi, mankhwala oledzeretsa ndi utoto (paint). Zopangidwazo zimakhala zoyera. Zalembedwa mu ndemanga (yopangidwa ndi Suleymhan bin Abdullah Shi'ridi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" kwa Molla Halil Shi'ridi's "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" m'bukhu la **al-Ma'fuwat** kuti lamuloli likugwiranso ntchito m'Madhhab a Shafi'i. Sizingalepheretse Swalah (kukhala sahih) ngati pali haraj poziyeretsa. Mongolingalira kuti za madzi izi ndi zoyera potengera haraj (poziyeretsa), ndi kosaloledwa kumwa pokhapokha ngati pali darurat kutero. Zakumwa zoledzeretsa sizikhala za ukhondo. Pakuti mowa mu za kumwazi wasakanizidwa ndi zinthu zina osati pofuna kuthetsa ludzu kapena njala koma kusangalatsa basi. Chilichonse chomwe chapakidwa ndi zoterezi chimakhalanso najs. Ndi Haram nthawi zonse kuzimwa popanda darurat.]

MACHIMO AKULU
(GHUNAH-I-KEBAIR)

Pali machimo akulu amitundumitundu, omwe amatchedwa ghunah kabair. Makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri (72) mwa iwo ndi awa:

1– Kuphana mopanda chilungamo.

2- Kuchita chiwerewere

3- Mathanyula (kulowetsana pokhalira) ndi haram m'chipembedzo chirichonse.

4- Kumwa vinyo kapena chakumwa china chirichonse choledzeretsa.

5 - Kuba.

6- Kudya, kumwa kapena kufwenthera mankhwala osokoneza bongo.

7- Kulanda katundu wa eni pogwiritsa ntchito mphamvu kapena mwachinyengo.

8- Kuchitira umboni wonama.

9- Popanda 'udhr, kudya pamaso pa Asilamu ena m'mwezi wodalitsika wa Ramadhan.

10- Riba, -kubwereka kapena kubwereketsa katundu kapena ndalama pa chiwongola dzanja.

11- Kulumbira kawirikawiri.

12- Kusamvera makolo ako.

13- Kusiya kuchita sila rahm kwa mahram achibale omwe ndi a Salih Asilamu. (Sila-i-rahm ikutanthauza kuyendera abale ako mtima.)

14– Pa nkhondo, kuchoka pa nkhondo ndi kuthawa adani.

15- Kugwiritsa ntchito chuma cha ana amasiye popanda chilolezo cha ana amasiye. Zanenedwa motere chakumapeto kwa tsamba (266) (losindikizidwa kachikhumi) gawo la chisanu la **Endless Bliss**: "Woyang'anira amasiye asabweze ngongole za malemuyo ndi katundu wa ana amasiye. Ndiponso asapereke chopereka cha pa chuma cha mwana wa masiye, kapena kuchita Qur'ban ya ana amasiye (ndi chuma cha masiye). Koma atate (ake a mwana wa masiye) angathe. Ngati woyang'anira ali wosowa, amatha kugwiritsa ntchito chuma cha mwana wa masiyecho, koma sangathandizire nacho munthu wina."

16- Kusagwiritsa ntchito masikelo kapena miyezo yanu moyenera.

17- Kuchita Swalah za pa tsiku nthawi yake isanakwane kapena itatha.

18- Kupsyetsa mtima m'bale wanu wokhulupilira.

19- Kunena za bodza ponamizira kuti ndi mawu ochokera kwa Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" pomwe mawuwo si a Mtumiki.

20- Kulandira ziphuphu.

21- Kupewa kupereka umboni woona.

22- Osapereka zakat kapena ushr pa chuma chako.

23- Kumuwona munthu akuchita tchimo, koma osayesera kumuletsa ngakhale ungathe.

24- Kuwotcha nyama ili ndi moyo.

25- Kuyiwala kuwerenga Qur'an al azim koma utaphunzira (kuwerenga) kwake.

26- Kutaya chiyembekezo cha chifundo cha Allahu ta'âlâ.

27- Kuchitira chinyengo anthu atakukhulupirira; posatengera kuti anthuwo ndi Asilamu kapena si Asilamu.

28- Kudya nyama ya nkhumba, yomwe ndi haram.

29- Kuwada ndi kutembelera Sahabah wa Rasulullah ridwanullahi ta'âlâ 'alaihim ajma'in aliyense.

30- Kupitiriza kudya mutakhuta; ndi haram kutero.

31- Kwa mkazi, kupewa kugonana ndi mamuna wake (popanda chifukwa).

32- Kwa mkazi, kupita kukaonana ndi mnzake popanda chilolezo cha mamuna wake.

33- Kunamizira mkazi wolemekezeka kuti amachita za dama.

34- Kuchita miseche pakati pa Asilamu (Namima).

35- Kuwonetsa ziwalo zako za awrat kwa ena. [Ziwalo zobisika (awrat) za mamuna ndi zomwe zili pakati pa mchombo ndi mawondo ake. Tsitsi, mikono ndi miyendo ya mkazi nazonso zili mkati mwa ziwalo zake zobisika (awrat).] Kuwona maliseche a wina ndi tchimo.

36- Kudya nyama yotchedwa 'lesh' monga; nyama yololedwa kudya koma yoti yafa yokha kapena nyama yololedwa kudya imene yaphedwa m'njira yosagwirizana ndi mmene Chisilamu chimanenera.

37– Kuphwanya chikhulupiliro.

38- Kumujeda Msilamu.

39- Kukhala wa nsanje.

40- Kumuphatikiza Allahu subhanahu wa ta'âlâ ndi zinthu zina. (Mchitidwe woyipawu umatchedwa shiriki.)

41- Kunama.

42- Ukalikulire, kudziyesa wopambana.

43- Kuchotsa wolowa mmalo pa wasiyya yako utarsala pang'ono kufa.

44 - Kukhala waliuma ndi wa umbombo kwambiri.

45– Kukonda za pa dziko, [zomwe zili za haram]

46- Kusaopa mazunzo omwe adzaperekedwe ndi Allahu ta'âlâ.

47- Ngati chinthu chili haram, kusakhulupilira kuti ndi cha haram.

48- Ngati chinthu chili halal, kusakhulupilira kuti ndi cha halal.

49- Kukhulupilira zonena alozi olozera za mwayi wa anthu ndi za ghayb (zobisika ndi zamtsogolo).

50- Kusiya chipembedzo chako, nkukhala murtadd (ogalukira).

51- Kuyang'ana mkazi wa mwini kapena mwana wa mkazi wa wina popanda 'udhr kutero.

52- Kwa akazi kuvala zovala za chimuna.

53- Kwa amuna kuvala zovala za chikazi.

54- Kuchita machimo mkati mwa haram sharif.

55- Kuitana Adhan kapena kuchita Swalah nthawi ya swalah isanakwane.

56- Kusamvera akuluakulu a boma, kuphwanya malamulo.

57- Kufananiza ziwalo za Mahram za mkazi wako ndi ziwalo za mahram za amayi ako.

58- Kutukwana mayi a mkazi wako (apongozi ako).

59- Kulozerana mfuti.

60- Kudya kapena kumwa zotsalira zomwe galu amadya kapena kumwa.

61- Kumukumba (munthu) pa za bwino zomwe munamuchitira.

62- Kwa amuna kuvala zovala za siliki.

63- Kulimbikira kukhala wosazindikira. [Kusaphunzira Chikhulupiriro cha Ahl as-Sunnah, fardh, haram, ndi maphunziro a mtundu uliwonse wofunikira.]

64- Kulumbira potchula maina ena osakhala dzina la Allahu ta'âlâ kapena kutchula mayina ena kusiya omwe atchulidwa m'Chisilamu.

65- Kuthawa maphunziro (kudziwa).

66- Kusamvetsa kuti umbuli ndi chinthu choyipa.

67- Kupitiliza kupanga machimo ang'oang'ono.

68- Kuseka phwete popanda chifukwa chovomerezeka mchisilamu kutero (udhr)

69- Kukhala ndi janaba kwa nthawi yayitali zomwe zingakuchititseni kuphonya imodzi mwa swalah za pa tsiku.

70- Kugonana ndi mkazi wako pa nthawi yomwe ali pa nsambo kapena pa nthawi yomwe ali pa kuchira kwa ubereki.

71- Kupanga nyimbo yokometsera. Kuyimba nyimbo zoyipa, zolaula. Kuyimba ndi zida zoyimbira. Mirza Maz-har-i-Jan-i-Janan “rahima-hullâhu ta’âlâ”, m'modzi mwa akatswiri a Chisilamu opambana ku India, akunena motere m'bukhu lake lotchedwa **Kalimat-i-tayyibat**: "Ndi nkhani yoti akatswili a Chisilamu agwirizana kuti ndi haram kuyimba zida za mtundu uliwonse kapena kumvera pamene zikuyimbidwa. Pali mawu akatswiri akuti chitoliro ndi chida chokhacho chomwe chiri makruh kuyimba ndi kuti ndi mubah (kololedwa) kuyimba ng'oma pa ukwati.

[Pamene Qur’an al-karee ikuwerengedwa kapena kulakatulidwa mokweza mawu kapena Adhan ikuchitidwa mokweza mawu, zili haram ngati tanthauzo lake lasinthidwa kapena mawu abwerezedwa (moti mpaka kusintha tanthauzo). Zanenedwa motere m’bukhu la **al-Fiqh-u-’alal-Madhahib-ul-erba’a**: “Ndi haram kuchita Adhan mokometsera mawu. Sizololedwa kumvera zoterozo.” Zimatchedwa **taghanni** kapena **sima** kuwerenga (kapena kubwereza) mawu mokometsera. Taghanni imatanthauza kuyankhula, (kuwerenga kapena kubwereza) mokometsera liwu lomveka bwino kuti limveke mosangalatsa. Pali mitundu iwiri ya kuwerenga (kapena kulakatula) Qur'an al-kerim kapena kuchita Adhan kapena mawulidi kapena ilahis (kutamanda) ndi taghanni:

1- Taghanni yomwe ndi Sunnah ndipo yomwe imabweretsa thawab, (malipiro a tsiku lomaliza). Kuchita mogwirizana ndi phunziro lotchedwa 'tajwid' (lomwe limaphunzitsa kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kerim moyenera). Taghanni yamtunduwu imalimbikitsa mitima ndi miyoyo.

2- Taghanni yoletsedwa, ya haramu, ndi kuchita mokometsera ndikumamveka ngati kuti ndi nyimbo. Mtundu wa taghanni uwu umawononge tsa katchulidwe ka mawu. Umasokoneza mau ndi kusintha tanthauzo. Mamvekedwe a kachitidwe kake amakhala okoma ku Nafs al- ammara. Zimachititsa anthu kutengeka ndi nafs ndi kuyamba kulira ndi kukuwa, zomwe zimawachititsa kuti asathe kulingalira matanthauzo ake ndi kuwachititsa kuti zikhale zosatheka kuti mitima yawo ndi miyoyo yawo igonjetse kuyiwala ndi matenda.

Zanenedwa motere patsamba 162 la **Targhib-us-salat** lolembedwa ndi Muhammad bin Ahmad Zahid “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih”, yemwe anamwalira mu 632 [1234 AD] ku India,) komanso pa tsamba 1342 m’bukhu lachiwiri la **Bariqa** lolembedwa ndi Muhammad bin Mustafa Hadimi “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih”, yemwe anamwalira mu 1176 [1762 AD], Hadim, Konya, Turkey,) ndi pa tsamba 589 m'bukhu

lachiwiri la **Hadiqa** lolembedwa ndi Abd-ul-Ghani bin Isma'il Nablusi, 1050 [1640 AD7, Damascus - 1143 [1731], malo omwewo) “Musakwere nyama yomwe yakongoletsedwa ndi mabelu ndi cholinga chodzisangalatsa nokha, pakuti kutero ndi makruh. Pakuti, mabelu ndi zida zoyimbira za mdyerekezi. Angelo achifundo satsikira m’magulu apa ulendo (okhala ndi nyama) zokhala ndi mabelu.” Koma ndi kololedwa kutero pa bizinesi zina kapena pa zinthu zobweretsa phindu.

Pali kuvomerezana kwa akatswiri kuti ndi haram kuwerenga kapena kulakatula ndakatulo zosemphana ndi Chisilamu ndi chikhalidwe. Kuwerenga kapena kulakatula m'malo a fisq, komwe kuli zida zoyimbira ndi za kumwa zoledzeretsa kapena komwe amuna ndi akazi akusangalala pa modzi ngakhale ndakatuloyo ingakhale yogwirizana ndi Chisilamu ndi chikhalidwe chabwino. Ndi haram kukhala m’magulu osakanikirana amenewo ndikumamvera ndakatulo zomwe zikuchitidwa malo ena ndikumaulutsidwa pa wayilesi, pa wayilesi ya kanema kapena pa tepi rekoda. Ndi haram kuti amayi ndi anyamata aziyimba nyimbo zoterezi m'makorasi osakanikirana.]

Ndizololedwa kuwerenga kapena kulakatula ndakatulo zoyenera pa malo oyenera. Zikhoza kufewetsa mitima (ya omvera) ndikuchita zomwe zingadzetse chifundo cha Allahu ta’âlâ. Akatswiri ena samakopeka ngakhale ndi mtundu wa (kuyimba) wa mubah (wololedwa) wa sima’. Kusafuna kwawo sima’ kumachokera pa kunyansidwa kwao ndi zomwe zimachitika mu chikhalidw chawo. Koma kusagwirizana kwa chilengedwe kumeneku sikunachititse akatswiri odalitsidwawo kusavomera kapena kuwakana anzawo ofunika kwambiri omwe ankafuna kuchita sima. Ndi zoletsedwa kuwerenga kapena kulakatula Qur’an al-kareem kapena mawulidi kapena ilahis (kutamanda) kapena salawat sharifs (mapemphero apadera a Rasulullah ndi kuwatumiza ngati mphatso kwa mzimu wake wodalitsika) m'malo a fisq, ngakhale izi zitachitika mwa ulemu wonse. (Malo a fisq ndi malo amene machimo amachitika.) Ndi kufuru (kusakhulupilira) ngati zikuchitika pofuna kusangalatsa kapena kucheza. Kwalembedwa mu tsamba la chisanu ndi chimodzi la **Durr-ul-ma’arif** kuti: “Zida zoyimbira ndi mawu akazi ndi anyamata ndi ghina (nyimbo za machimo) ndi haram. Ndakatulo zothandiza ndi sima’ ndi mubah, koma pokhapokha ngati zitachitika mmalo abwino komanso ndi mawuabwino"

72- Kudzipha, kutanthauza kudzipha wekha ndi tchimo lalikulu kuposa kupha. Munthu wodzipha amazunzidwa ndi zilango za kumoto kuyambira m'manda.

Ngati sakufa nthawi yomwe wafuna kudzipha ndipo achita tawba, machimo ake onse adzakhululukidwa. Sadzazunzika m'manda mwake. [Kuti Tawba yomwe wachita utaphoya swalah ikhale sahih ndi kuchita qada. Munthu amene wayamba kuchita qada (ya Swalah zomwe anasiya) wachita niyyah kuti achite mapemphero a qada mpaka kumapeto kwa moyo wake. Ndi niyyah yakeyo, ngongole zake zonse za qada zidzakhululukidwa. Chimodzimodzi, munthu wosakhulupilira akakhala Msilamu ndi kuchila tawba chifukwa chokhala wosakhulupirira kapena chifukwa choti amakanira pochita bid'at, iye wachita niyyah kuti sadzayambiranso ukafiri ndi kukanira, ndipo kuti sadzamberezanso kuchita zoyipa zimene anali kuchita m'masiku akale a umbuli. Ndi niyyah yawo imeneyi, machimo awo onse amakhululukidwa.]

MALISECHE (AWRAT) ndi KUZIPHIMBA KWA AZIMAYI

Zanenedwa motere m'mutu wokamba za 'nikah (mgwirizano wa ukwati wovomerezeka m'Chisilamu)' m'buku lotchedwa **Eshi'at-ul-leme'at** lolembedwa ndi 'Abd-ul-Haqq Dahlawi' "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", 958 [1551 AD] - 1052 [1642]):

1- Abu Hurayra "radiyallâhu anh" akuti: Munthu wina anabwera kwa Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" nati: Ndikufuna kukwatira mtsikana wa ku Answar." Mneneri wodalitsika adati: "**Muone mtsikanayo** [kamodzi]. **Pali china chake m'maso mwa** (anthu a) **mtundu wa Ansari**." Hadithi sharif iyi yalembedwa m'bukhu lotchedwa **Sahih Bukhari**. Ndi Sunnah kumuona kaye ka modzi mtsikana yemwe ukufuna kumukwatira.

2- Abdullah ibni Masud "radiyallâhu anh" anati: "**Akazi sayenera kuwauza amuna awo za kukongola ndi ubwino wa akazi ena amene akhala akuwaona. Zidzakhala ngati kuti amuna awo anawaona akazi amenewo**." Hadithi sharif iyi yalembedwa m'mabuku otchedwa **Sahih Bukhari** ndi **Sahih Muslim**.

3– Abu Said Hudri "radiyallâhu 'anh" (d. 64 [683 A.D.]) akuti: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ananena kuti: **"Mamuna sayenera kuyang'ana maliseche a mamuna wina, ndipo mkazi sayenera kuyang'ana maliseche a mkazi wina!"** Apa zikuonekeratu

kuti ndi haram kwa amuna kuyang'ana ziwalo za awrat za akazi ngati mmenenso zirili haram kwa akazi kuyang'ana ziwalo za awrat za amuna, ndipo ndi chimodzimodzi ndi haram kwa amuna kuyang'ana ziwalo za awrat za amuna ena ndiponso kwa akazi kuyang'ana ziwalo za awrat za akazi ena. Ziwalo za awrat za mamuna (zomwe ziri haram) kwa amuna ena kuziona ndi zomwe ziri pakati pa mawondo awo ndi mchombo. Lamulo lomweli layikidwanso kwa akazi. Tsono ziwalo za awrat za mkazi (zomwe ndi haram) kwa amuna kuziona ndi thupi lake lonse kupatula manja ndi nkhope. Ndichifukwa chake, akazi amatchedwa awrat. Kaya mkaziyo ndi Msilamu kapena sali Msilamu, koma ndi haram kwa mamuna kuyang'anitsitsa nkhope ya mkazi yemwe ndi na-mahram wake ndi shahwa (chilakolako), ndipo ndi haram kuyang'ana ziwalo zake za awrat ngakhale popanda chilakolako.

4- Jabir bin Abdullah "radiyallâhu anh" (yemwe anaphedwa mchaka cha 74 [693 AD]) anati: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam"adati: "**Musagone m'nyumba ya mkazi yemwe ali na-mahram kwa inu!**"

5- Aqaba bin Amir "radiyallâhu anh" akunena: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: "**Musakhale mchipinda chanokha ndi mkazi yemwe ali na-mahram kwa iwe! Ngati mkazi akhala mchipinda chayekha ndi m'bale wamamuna wa mamuna wake kapena mwana wamamuna wa mamuna wake, iye adzakokeredwa ku imfa."** Kutanthauza kuti iye amayambitsa fitna ndipo zotsatira zake ndi chisokonezo. Izi ndi zoyenera kuzipewa mwa njira iriyonse. Hadithi sharif iyi yalembedwa mu **Sahih Bukhari** ndi mu **Sahih Muslim**.

6- Abdullah ibni Mes'ud "radiyallâhu anh" akunena: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Thupi la mkazi ndi awrat (maliseche)."** Kotero liyenera kuphimbidwa. **"Mkazi akatuluka mnyumba, satana amamuyang'ana nthawi zonse."** (Satana amamugwiritsa ntchito ngati nyambo yonyengelera amuna ndi kuwatsogolera ku machimo.)

7- Burayda "radiyallâhu 'anh" akunena: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam"anati kwa Hadrat Ali: **"Oh iwe Ali! Ukawona mkazi tembenuza nkhope yako ndikupewa kumuyang'ana iye. Osamuyang'ana kachiwiri! Si tchimo kumuyang'ana mosayembekezera. Koma ndi tchimo kumuyang'ana kachiwiri."** Zinanenedwa ndi Abu Dawud komanso ndi Darimi.

8- Ali "radiyallâhu 'anh" akunena: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Oh iwe Ali! Usaonetse ntchafu yako, ndipo**

usayang'ane ntchafu ya wina, wakufa ngakhale wamoyo!" Hadith sharif iyi inanenedwa ndi Abu Dawud ndi Ibni Maja. Kotero, kuyang'ana maliseche a munthu wakufa kuli ngati kuyang'ana maliseche a munthu wamoyo. [Tiyenera kuchita zotheka kupewa kuona ziwalo zobisika za anthu ochita masewero ndi osambira.]

9– Abdullah ibni Umar "radiyallâhu 'anhuma" (d. 73 [692 A.D.] Mekka) akufotokoza: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati**: "Musamaonetse ziwalo zanu zobisika!** [Musawonetse ngakhale mutakhala nokha.] **Pakuti pali zolengedwa zomwe sizimakusiyani inu kukhala nokha. Chitani manyazi pamaso pa zolengedwa zimenezi ndi kuzilemekeza!** Awa ndi angelo otchedwa Hafadha, omwe amakutetezani ku majini. Iwo amakusiyani nokha nthawi ziwiri zokha, nthawi yomwe muli ku chimbudzi ndi nthawi yomwe muli pachikondi ngati mamuna ndi mkazi.

10- Umm-i-Salaama "radiyallâhu 'anha" akufotokoza kuti: Iye ndi Meymuna "radiyallâhu 'anha" anali ndi Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam"pamene Ibni Umm-i-Maktum "radiyallâhu 'anh" anapempha chilolezo kuti alowe ndipo analowa. Pamene Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" anamuwona anati kwa ife: **"Khalani kuseri kwa katani lotchinga!"** Pamenepo ine ndinati, "Kodi iye si wakhungu? Sangatiwone," "**Kodi inunso ndinu akhungu? Inu simungamuone?"** anatero wolengedwa opambana mwa zolengedwa zonse. Mmawu ena, Iye amati: "Kukhala kwake wa khungu sikudzachititsa inunso kukhala akhungu. Hadithi sharif iyi yalembedwa ndi Imam Ahmad ndi Tirmizi komanso ndi Abu Dawud "rahima-hullâhu ta'âlâ". Malinga ndi Hadithi sharif iyi, monga momwe ziliri kwa mamuna kuyang'ana mkazi yemwe ali na-mahram kwa iye, chimodzimodzinso nkosaloledwa kwa mkazi kuyang'ana mamuna yemwe ali na-mahram kwa iye. Ma Imam (akatswiri) a m'Madhhab athu onse anayi "rahima-hullâhu ta'âlâ", ponganizira Hadith isharif zina, anati: "Ndizovuta kuti mkazi asayang'ane mutu ndi tsitsi la mamuna yemwe ali na-mahram wake. Malamulo ovuta kuchita ndi **azimats**. Kwa mkazi, ziwalo zobisika za mamuna ziri pakati pa mawondo ake ndi mchombo. Ndi kosavuta kupewa kung'ana mbali zimenezo. Malamulo osavuta kuchita ndi **rukhsat**.

[Monga taonera, Ezwaj-i-tahirat (akazi oyera a Mtumiki wathu wodalitsika, omwenso ndi azimayi a Chisilamu), "radiyallâhu ta'âlâ 'anhuma" ndi Sahabah-i-kiram "radiyallâhu 'anhum" amakonda njira ya 'azimats ndikupewa rukhsat. Maganizo opanda nzeru omwe akuti akazi "samaziphimba matupi awo mu nthawi ya Mtumiki. Zomwe

masiku ano tikuwona azimayi akuziphimbazi kunalibe nthawi imeneyo. Hadrat' Aisha weniweniyu amayenda wopanda mpango ku mutu. Ndipo kuti chikhalidwe cha makono choziphimba akazi chinayambitsidwa pambuyo ndi anthu opotoka maganizo ndi anthu a fiqh," ndi kuyankhula kwa mwano komwe anachita achiwembu a ku Britain amene cholinga chawo chenicheni chinali chowononga Chisilamu pochokera mkati mwa Asilamu eni ake ndi **azindiq.** Ndi zowona kuti kuziphimba kwa akazi sikunali lamulo la Chisilamu kalelo. Inali nthawi ina pakati pa chaka cha chitatu ndi cha chisanu cha Hijira pamene akazi analamulidwa kuti azidziphimba okha. M'bukhu lake la chi Turk lotchedwa **Tacrid-i-sarih Tercemesi,** Babanzada Ahmad Na'im Begh (1290 [1872 A.D.] – August 14th 1352 [1934], Edirnekapı, Istanbul) akulemba kuti: Ma ayat a hijab (kudziphimba kwa akazi) avumbulutsidwa katatu kosiyana.]

11- Behz bin Hakim, mmodzi mwa anthu olemekezeka kwambiri mwa ma Tabi'in, akufotokoza kuchokera kwa atate ake ndi agogo ake kuti: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ananena**: "Phimbani ziwalo zanu zobisika! Musalole aliyense kuziwona, kupatula mkazi wanu ndi ma jariyas! Chitaninso manyazi pamaso pa Allahu ta'âlâ!"** Hadithi sharif iyi inanenedwa ndi Tirmidhi, ndi Abu Dawud, ndi Ibni Maja "rahima-hullâhu ta'âlâ". Jariya imatchedwa **mulki-yemin**, ndipo tanthauzo lake ndi, mulk (katundu) wa dzanja la manja. Pakuti, jariya imayesedwa ndi dzanja la manja pogula, ndipo ndalama za jariya zimaperekedwa ndi dzanja lamanja.

12- Umar-ul-Faruq "radiyallâhu 'anh"akunena: Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Ngati mamuna achita halwat ndi mkazi yemwe ali na-mahram kwa iye,** (kutanthauza kuti ngati akhale limodzi m'chipinda popanda wina aliyense,) **Satana amakhala nawo ngati munthu wachitatu."** Hadithi sharif iyi idanenedwa ndi Tirmidhi. [Ndi haram kuchita halwat ndi mkazi yemwe ndi na-mahram. Mamuna ndi mkazi asakhale awiriwiri malo obisika, otseka. Mu zolemba zake za nkhani yokhala imam, Ibni Abidin akunena motere: "Ngati pali wa chitatu mamuna kapena mkazi yemwe ndi pa chibale chenicheni ndi mmodzi mwa iwo wotchedwa **zi-rahm-i-mahram**, kukumanako sikudzakhala halwat."]

13- Jabir bin Abdullah "radiyallâhu 'anh" anati: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" akunena: "**Musakawachezere akazi amene amuna awo achoka! Pakuti** (ngati mungatero) **Satana adzayendelera m'mitsempha yanu ngati magazi**." Atamufunsa kuti: "Kodi satana angayendelerenso mwa inu?" Wokondeka wa Allahu

ta'âlâ anayankha: "Inde. Angayendelerenso mwa ine. Koma Allahu ta'âlâ wandithandiza polimbana naye. Amuchita kukhala Msilamu kotero moti wadzipereka yekha kwa ine. Hadithi sharif iyi yanenedwa ndi Tirmidhi "rahima-hullâhu ta'âlâ".

14- Umm-i-Salaama "radiyallâhu 'anha" akunena: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anali ndi ine (m'chipinda changa). Munalinso kapolo wa mchimwene wanga Abdullah bin Abi Umayya. Kapoloyo anali muhanneth (mamuna wowoneka ndi kuyankhula ngati mkazi). Pomwe Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" anamuwona Muhannath uja ndikumva mawu ake anati: **"Musamawalowetse anthu monga ameneyu m'nyumba mwanu!** Hadithi sharif iyi yalembedwa mu **Sahih Bukhari** ndi **Sahih Muslim**.

Amuna omwe amavala, kuyankhula ndikuchita ngati mkazi ndi otembeleredwa. Hadithi sharif ikunena motere za iwo: **"Allahu subhanahu wa ta'âlâ awadzudzule amuna omwe amadzifanizira kuti awoneke ngati akazi ndi akazi omwe amachita zodzifanizira ngati amuna!"** Akazi amene amavala zovala za chimuna ndi kumeta tsitsi lawo ngati amuna ndikuchita zomwe amuna amachita komanso amuna amene amasunga tsitsi lalitali ngati mkazi ndi kudzikongoletsa ngati akazi, popanda 'udhr yowakakamiza kutero, ndi amene akunenedwa mu Hadithi sharif iyi. Misver bin Mahrama "radiyallâhu 'anh"anabadwa m'chaka chachiwiri cha Hijra. Iye ndi mwana wa mlongo wake wa Abd-ur-Rahman bin Awf "radiyallâhu 'anhuma" . Iye akulongosola kuti: Ndinali nditanyamula mwala waukulu, pamene zovala zimene ndinavala zinatsetserekera pansi. Ndinalephera kuti ndizikwezere mmwamba. Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anandiwona ndili choncho. **"Kwezera zovala zako mmwamba! Osatuluka wopanda chophimba!"** Hadith sharif iyi yalembedwa mu **Sahih Muslim**. Hadithi sharif iyi imaletsa amuna ndi atsikana kukhala osavala m'misewu kapena m'mphepete mwa nyanja kapena m'mabwalo amasewero.

16- Abu Umama "radiyallâhu 'anha" akufotokoza kuti, Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ananena kuti: **"Ngati mamuna awona kukongola kwa mtsikana ndipo iye athawitsa nkhope yake kuti asawonenso, Allahu subhanahu wa ta'âlâ amampatsa thawab za ntchito yatsopano yopembedza ndipo nthawi yomweyo amasangalala ndi kukoma kwake kwa thawabuzo."** Hadithi sharif iyi yalembedwa ndi Imam Ahmad bin Hanbal "rahima-hullâhu ta'âlâ".

17- Hasan Basri "rahmatullâhi 'alaih"akulongosola za Hadith mursel: kuti Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ananena kuti :

"Allahu subhanahu wa ta'âlâ akupereka chidzudzulo kwa munthu amene amaonetsa ziwalo zake zobisika ndi yemwe amayang'ana ziwalo zobisika za wina!" Hadith shrif iyi yalembedwa m'buku la Imam Bayhaki lotchedwa Shu'ab-ul-iman.

18- Abdullah ibni Umar "radiyallâhu 'anhuma" akunena kuti Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: "**Ngati munthu adzifananiza ndi mtundu wina (gulu la anthu), adzakhala mmodzi wa iwo!"** Hadith sharif iyi yalembedwa ndi Imam Ahmad ndi Abu Dawud "rahima-hullâhu ta'âlâ". Izi zikutanthuza kuti ngati kalidwe la munthu, zochita zake, kapena zovala zomwe amavala azichita kukhala zofanana ndi za adani a Chisilamu, iye adzakhala mmodzi mwa adani a Chisilamu. [Hadith sharif iyi ndi chenjezo kwa anthu omwe amakonda zinthu zatsopano zomwe osakhulupilira ayambitsa, ndi kuchula zinthu za haram kuti ndi 'fashion' (zamakono), ndikuwatcha ochita za haram kuti ndi akatswiri pa zochitachita.

19- Amr Shu'ayb akuyankhula ndi umboni wochokera kwa atate ake ndi agogo ake kuti Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam"anati: **"Allahu subhanahu wa ta'âlâ amakonda kuwona mphatso zomwe wapereka kwa kapolo Wake."** Hadithi sharif iyi yanenedwa ndi Tirmidhi "rahima-hullâhu ta'âlâ". Tikamvetsetsa, Allahu ta'âlâ amakonda kuti zovala za munthu zikhale za ukhondo ndi zoyera. IYE amakonda yemwe amapanga kapena kusoka ndi yemwe amavala kuti asonyeze mphatsoyo. Amadana ndi anthu amene amapanga ndi ovala (zovala) zopangidwa ndi cholinga choyesa ndi kukwaniritsa zofuna za chabe. Ndikosaloledwa kubisa mphatso yoperekedwa ndi Allahu ta'âlâ. Maphunziro ndi mphatso yoperekedwa ndi Allahu ta'âlâ.

20- Jabir bin Abdullah "radiyallâhu anh" akunena kuti: Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" anabwera kwathu. M'nyumbamo munali munthu wina yemwe anali ndi tsitsi losasamalika. Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" atamuona anati: "**Kodi iyeyu walephera kupeza chinachake choti akadatha kugwiritsa ntchito kusamalira tsitsi lake"** Atawona wina atavala zakuda anati: **"Kodi iyeyu wasowa chinachake choti akanatha kuchapira zovala zake?"**

21- Mmodzi mwa Tabi'in, Abu-l-ahves, akulongosola ndi umboni wochokera kwa atate ake kuti: Ndinapita ku malo kwa Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam". Zovala zanga zinali zakale komanso zong'ambika. Iye anafunsa, **"Kodi ulibe chuma."** Ndinati ndili ndi chuma. Anafunsanso kuti: **"Uli ndi chuma chotani? "**Ndili ndi chuma cha mtundu uliwonse," ndinatero. Pamenepo wolengedwa wapamwamba pa zolengedwa zonse anati: **"Allahu subhanahu wa**

ta'âlâ akakupatsani chuma, amafuna kuwona zipatso zake pa inu." Hadith sharif iyi yalembedwa ndi Imam Ahmad ndi Nasai "rahima-hullâhu ta'âlâ". Apa tamaliza kumasulira kwathu kuchokera mu gawo la chitatu la buku lotchedwa **Eshi'at-ul-leme'at.**

22- Zanenedwa motere m'buku la Yusuf Qardawi lotchedwa **al Halaluwal-haramu-fil-islam**: "Chipembedzo cha Chisilamu chikuletsa mkazi kuvala zovala zopyapyala zowonetsa za mkati. Zanenedwa motere mu Hadith sharif yomwe yatchulidwa m'mabuku a **Sahih-i-Muslim** ndi **Muwatta** kuti: **"Akazi omwe avala (koma) nkumaoneka kuti ali maliseche ndi akazi oyimika mitu yawo ngati linunda la ngamira sadzalowa ku Mparadiso. Sadzalandira ngakhale fungo la ku Mparadiso. Fungo la ku Mparadaiso limafika kutali kwambiri."** Hadith sharif iyi imaletsa akazi kuvala zovala zothina, zowonekera mkati, matiyitsi, ndi zipewa za manyado mmutu. Ikuletsanso kupota tsitsi ndi kulikulunga pa mutu ngati mpira, komanso ikuletsa kumanga tsitsi logula. Kuchita izi ndi tchimo chimodzimodzi ngati kuyenda maliseche. Azimayi ndi atsikana a Chisilamu sayenera kuvala zovala zopyapyala ndi zothina ndipo sayenera kupota tsitsi lawo kapena kuvala tsitsi logula. Asakulunge tsitsi lawo pa mutu ngati mpira. Ayenera kudziwa kuti machismo awa ndi oyipa moti angakamutengere munthu ku Jahannama.

[Tanena kale za Qardawi kuti ndi munthu wopembedza koma osatsatira Madhhab aliwonse. Ndi fardh ndipo zalamulidwa m'chipembedzo cha Chisilamu kuti akazi azivala bwino ndipo chafotokoza bwino momwe akazi ayenera kuvalira ndi zomwe ayenera kuvala. Kufotokozaku sikukunena za mtundu wa nsalu zovala, kapena mtundu wa diresi, kapena siketi kapena koti. Zalembedwa m'mabuku a Fiqh kuti ndi fardh kwa akazi kuvala (monga zalongosoledwa). Koma mitundu ya zovala zogwiritsa ntchito ndi madiresi ovala ndi nkhani ya **Sunnah-i-zawaid**, yomwe nayonso imatengera Sunnah zokhudzana ndi miyambo osati kulambira. Pachifukwa ichi, mtundu wa zovala uyenera kukhala wa zovala za chikhalidwe. Ndi makruh kusalemekeza mwambo mu zinthu zosakhudzana ndi kupembedza. Kunena zowona ndi haram ngati zingayambitse fitna. Kwanenedwa mu **Hindiyya** kuti: "Ndi zololedwa kuyang'ana mkazi atavala chinthu chokhuthala ndi chokwanira. Koma sizololedwa kuyang'ana mkazi wovala zothina. Ndi haram kuyang'ana mwachilakolako nkhope ya mkazi yemwe wavala (bwino) modzilemekeza. Ndi makruh kutero ngakhale popanda chilakolako ngati palibe chifukwa chochitira zimenezo. Lamulo lomweli likugwiranso ntchito poyang'ana akazi omwe si Asilamu.

Ndikololedwa kuyang'ana tsitsi lawo lokha, malinga ndi kunena kwa akadaulo ena a maphunziro."

Ndi bwino kwambiri kuvala malaya osathina, okhuthala, a mtundu wakuda onse ofikira mpaka m'mafupa a chidendene, ophimba mkono mpaka poyambira manja. Ndi bwino kuposa kuvala chovala chotchedwa charshaf chomwe ndi chopangidwa mzigawo ziwiri (siketi ndi bulauzi). Zanenedwa mu **Halabiyi-kebir** kuti: "Tsitsi la mkazi wa Chisilamu yemwe ndi mfulu, lotalika ndikugwera m'makutu mwake ndi mbali ya maliseche ake, malinga ndi kuvomerezana kwa pakati pa akatswiri a Chisilamu ena. Koma akatswiri a Chisilamu ochuluka amati mbali yokhayo yomwe ikupitilira m'munsi mwa makutu ndi maliseche. Malinga ndi kunena kwa akatswiri ena, mbali yolendewera si maliseche pa nthawi ya Swalah. Koma ndikosaloledwa kwa mamuna yemwe ali na-mahram kwa iye kuyang'ana mbali imeneyo." Ayenera kuphimba tsitsi lonse ndi nsalu yokhuthala. Kutsogolo kwa mpango womwe wavala kumutu kuchokera chapakati pake kuyenera kufika pa chipumi ndi kufika mpaka nsidze zake. Mmbali zonse ziyenera kufalikira mpaka polekezera kunja kwa nsidze zake ndi kutembenukira pansi ndi kutsika mpaka pa chibwano chake ndipo nsonga zake zilendewere mpaka pa mabere. Kumbuyo kwa mpangowo chapakati pake utsetsereke cha ku mtunda kwa nsana. Ngati kuli koti zingayambitse fitna, masaya nawonso ayenera kuphimbidwa. Ayeneranso kuvala masitonkeni okhuthala komanso oderako. Ngati gawo limodzi mwa magawo anayi a tsitsi lolendewera la mkazi likuwonekera kwa nthawi yokwana rukn imodzi (mu Swalah), Swalah yomwe achite sidzakhala sahih. Ndipo idzakhala makruh ngati kagawo kakang'ono kakhala kowonekera. Palibe bukhu la Chisilamu lomwe likusiyanitsa akazi akulu ndi ang'ono.

Pali akadaulo a Chisilamu amene anenapo kuti ndikololedwa kuvomera malonje a mayi wokalamba kapena kuchita naye musafaha (kugwirana naye chanza) kapena kuchita naye halwat, (kukhala naye m'chipinda chotseka); komabe palibe kadaulo aliyense wa Chisilamu amene wanena kuti ndikololedwa kwa mkazi wokalamba kusaphimba tsitsi lake kapena (kwa amuna amene ali na-mahram kwa iye) kuwona tsitsi lake (imvi). Akadaulo ena a Chisilamu anena kuti ndi kololedwa kuyang'ana tsitsi la mkazi yemwe sali Msilamu. Koma palibe m'modzi mwa iwo amene wanena kuti ndikololedwa kuwona tsitsi la mayi wa Chisilamu wokalamba. Akadaulo a Chisilamu omwe amanena kuti ndikololedwa mayi wokalamba kulowa mu mzikiti kapena kupita ku manda anena kuti tsitsi lake liyenera kuphimbidwa.

Sizolondola kunena kuti, “Zanenedwa mu ayat ya makumi asanu ndi anayi ndi mphambu zisanu ndi zinayi (97) mu Surah Ahzab kuti akazi a Chisilamu azidziphimba ndi **jilbab**. Ayat iyi ikuwalamula kuti azidziphimba ndi charshaf, yomwe ili ndi magawo awiri." Ngati ayah iyi inalamula (akazi) kuvala charshaf, akazi odalitsika a Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” ndi akazi a ma Sahabah “radiyallâhu ta’âlâ ’anhum ajma’in” akanavala charshaf. Koma palibe bukhu la Chisilamu lomwe likunena kuti aliyense wa iwo anavala charshaf. Bukhu la ku Turkey la Tafsir la mutu wakuti **Tibyan** likulongosola ayah iyi ngati lamulo lakuti akazi “ayenera kuphimba mitu yawo.” Zanenedwa m’bukhu la Tafsir lotchedwa **Jalalayn** kuti, (jilbab,) ndi chovala chimene akazi amavala ku mutu m’njira yoti chimaphimba nkhope yawo. Sawi akufotokoza zimenezi, ponena kuti: “Chovalacho chiri ndi chophimba kumutu ndi dhir’, (nsalu yomwe imayikidwa pamwamba pa chovala.)

Zinalembedwa motere m’mabuku a Tafsir otchedwa **Ruh-ul-beyan** ndi **Abu-s-su’ud**: “Jilbab ndi chovala ku mutu chomwe chimakhala ndi chingwe chimene amachikulunga ku mutu kuti tsitsi lisamagwedere; jilbab ndi yokulilapo mchithandi chomangira; imafika mpaka pa chifuwa ndi kutseka jayb, [kutseguka kwa pakhosi, ndi pa chifuwa,) kwa chovala. Mu ayah karima imeneyi, akazi akulamulidwa kuphimba mitu yawo ndi matupi awo onse.”

Mabuku a **Zewajir** ndi **al-Fiqh-u'ala-l-madhahib-ul-erba'a** akutchula Hadith sharif yosonyeza kuti jilbab ndi (chovala chomwe) chimavalidwanso ndi amuna ndipo akufotokoza kuti jilbab ya amuna ndi chovala chachitali chotchedwa qamis (chemise). Chovala cha akazi akamatuluka mnyumba chimayenera kukhala malaya atali ndi chomanga ku mutu chokhuthala chotchedwa charshaf ndipo chopangidwa ndi magawo awiri ofanana pokwaniritsa lamulo lokhudza kudziphimba kwa akazi lomwe latchulidwa pamwambapa.

Azimayi ayenera kudziphimba okha mogwirizana ndi miyambo yakudera la kwawo kuti asayambits fitna. Zalembedwa patsamba 26 la m’bukhu la **Sahih-i-Bukhari** kuti gawo lina la ayah lolamula akazi kuphimba ziwalo za awrat zawo linavumbulutsidwa pa tsiku la nikah ya Zaynab “radiyallâhu ’anha”. Nikah imeneyi inachitika m’chaka cha chitatu cha Hijira.]

Munthu yemwe amadzitcha Msilamu ayenera kudziwa kuti chinthu chirichonse chomwe angachite chikhale chogwirizana ndi Chisilamu. Ngati sakudziwa, ayenera kuphunzira pofunsa akadaulo a Ahl as-Sunnah kapena kuwerenga mabuku olembedwa ndi akatswiri otere.

Ngati zimene akuchita ndi zosagwirizana ndi Chisilamu, sangakhale otetezeka ku utchimo kapena ku zinthu zosakhala za chipembedzo. Tawba yeniyeni iyenera kuchitika tsiku ndi tsiku. Allahu ta'âlâa adzakhululuka tchimo kapena ntchito zotsutsana ndi chipembedzo ngati tawba itachitika. Ngati tawba siinachitike, kudzakhala kuzunzika pa dziko lapansi ndi ku Jahannama; zilango zidzakhalapo. Zilango zomwe zidzayenera kuperekedwa zalembedwa m'malo osiyanasiyana a bukhu lino.

Ziwalo za m'thupi za amuna kapena akazi zomwe ziyenera kuphimbidwa pochita Swalah ndi pena paliponse zimatchedwa **ziwalo za awrat**. **"Ndi haram kuwonetsa mbali zobisika za munthu kapena kuyang'ana mbali zobisika za ena."** Ziri Sunnah kwa munthu kuphimba mapazi ake (monga kuvala masokosi) pochita Swalah.

Munthu amene akunena kuti kulibe ziwalo za Awrat mu Chisilamu amakhala kafiri. Chipembedzo chathu chimatilamula kuti tiziphimba awrat zathu. Malo omwe pali mamuna ndi mkazi omwe ziwalo zawo zobisika zikuonekera kapena pomwe zida zoyimbira zikuyimbidwa kapena pomwe anthu akutchova njuga kapena pomwe zakumwa zoledzeretsa zikumwedwa kapena anthu akumvetsera pomwe mzimayi akuyimba amatchedwa **malo a fisq**. Ndi chinthu cha haram kupita kumalo a fisq. Mtimanso uyenera kukhala oyera. Kuyera mtima kumatanthauza kukongola muchikhalidwe. Mtima umayeretsedwa pomvera ndikutsatira chiphunzitso cha Chisilamu. Anthu amene samvera Chisilamu sangakhale ndi mitima yoyera. Munthu amenena akuti ndi 'halal,' kuonetsa chimodzi mwa ziwalo za thupi zomwe zimanenedwa kuti ndi awrat ndi ijma' (zomwe amavomerezana akatswiri onse a Chisilamu), zomwe zili awrat m'Madhhab onse anayi, kapena kuyang'ana ziwalo zobisika za ena ndiye kuti sawopa kuzunzidwa chifukwa cha tchimolo, ndipo iye amakhala wosakhulupilira. Lamulo lomweli limagwiranso ntchito kwa akazi omwe amawonetsa awrat zao, poyimba kapena kuchita maulidi pamaso pa amuna. Ziwalo za thupi la mamuna zomwe ziri pakati pamawondo ndi mchombo sizili awrat mu Madhhab a Hanbali mokha.

Munthu amene akuti, "Ine ndine Msilamu," akuyenera kuphunzira zofunikira za iman, za Chisilamu, fardh ndi haram zomwe madhhab onse anayi anaphunzitsa mogwirizana, chomwe ndi chiphunzitso cha ijma' (chovomerezana) ndipo nkofunika kuzilemekeza kwambiri. Kusazidziwa si udhr . Ziri ngati kuzidziwa ndikuzikana. **"Thupi lonse la mkazi, kupatula nkhope yake ndi manja ake, ndi awrat,** (liyenera kuphimbidwa,) **m'Madhhab onse anayi."** Msilamu akawonetsa

poyera mbali ina ya thupi lake yomwe ilibe ijma', yoti si awrat malinga ndi mmodzi mwa Madhhab atatu enawo, ndiye kuti wachita tchimo lalikulu malinga ndi zomwe wachita ku madhhab ake, ngakhale kuti sadzakhala kafiri (osakhulupilira). Chitsanzo cha izi ndi kuwonekera kwa ziwalo za amuna za pakati pa mawondo awo ndi pa mchombo. Ndi fardh kwa Msilamu kuphunzira zomwe sakuzidziwa. Akaphunzira zimenezo ayenera kuchita tawba nthawi yomweyo ndikuphimba chiwalo chawocho.

ZOMUYENEREZA WOKHULUPILIRA

Pali zinthu zisanu ndi ziwiri zomwe wokhulupilira ayenera kumuchitira wokhulupilira wina:

Akayitanidwa ayenera kupita;

Msilamu akadwala apite akamuone (Iyadat)

Pakachitika maliro apite akakhale nawo ndi kutenga gawo pa maliro.

Kumulangiza pofunika malangizo.

Akakumana ndi Msilamu mzake, kumulonjera.

Kumupulumutsa kwa opondereza ndi a nkhanza.

Kunena kuti, “Ya-r-hamukAllahu ta’âlâ,” akayetsemula kenako nkunena kuti, “Al-hamd-u-lillah.”

Wokhulupilira wabwino ndi amene mwa iye muli makhalidwe asanu ndi limodzi awa:

Amapembedza. Amaphunzira kuti adziwe. Sachita zoyipa. Amapewa za haram (zoletsedwa). Sawona katundu wawina ndi diso loyipa. Sayiwala imfa.

Zindikirani: Zanenedwa mu Hadith sharif kuti: **“Aliyense adzakonda anthu amene akuwachitira zabwino. Kukonda kumeneku ndi kwa chibadwa mwa munthu.”** Munthu amene amalola kulamulidwa ndi zilakolako za thupi lake amakonda anthu amene amamuthandiza kukwaniritsa zofuna za thupi lake. Munthu wa nzeru ndi wodziŵa zinthu, kumbali ina, adzakonda anthu amene amamuthandiza kukhala munthu waphindu.

Mwachidule, anthu abwino adzakonda anthu abwino. Anthu oyipa adzakonda anthu oyipa. Munthu mmene alili amadziwika ndi anthu omwe amakondana nawo ndikupanga nawo ubwenzi. Tiyenera kulemekeza aliyense powonetsa nkhope yomwetulira ndi mawu okoma. Izi tichitire bwenzi ngakhale mdani, Msilamu kapena osakhala

Asilamu; koma tisachitire anthu a bidah. Chisomo chofunika kwambiri kupereka kwa anthu komanso mphatso yamtengo wapatali kwambiri ndiko kuyankhula nawo mokoma mtima ndi kuwamwetulira. Tikawawona anthu akulambira ng'ombe, tiyenera kudyetsa udzu ng'ombeyo, potero tidzachotsa udani wawo kwa ife. Tisakangane ndi wina aliyense. Mikangano idzasokoneza ubwenzi ndi kukulitsa udani. Tisakwiyire aliyense. Mkwiyo umayambitsa litsipa ndi matenda a mtima. Hadith sharif ikuletsa kuti: "**Musakwiye!** (Mu Hadith sharif iyi Mtumiki wodalitsika akutilangiza kuti tipewe mkwiyo.)

Munthu adzakhala wabwino (ndi wothandiza) ngati angabise zinthu zinayi izi:

1- Umphawi wake;

2- Ntchito zake za chifundo;

3- Zowawa zake;

4- Mavuto ake.

Anthu anayi awa ndi aku Mparadiso:

1- Munthu amene lilime lake limachita dhikr.

2- Munthu amene ali hafid kalamullah (yemwe amasunga mawu a Allahu ta'âlâ).

3- Munthu wopatsa anthu chakudya.

4- Munthu amene amasala kudya m'mwezi wodalitsika wa Ramadhaan.

Munthu aliyense asaleke kutchula mawu asanu ndi awiri alembedwa pansipawa:

Anene **"Bismillah-ir-Rahman-ir-Rahim"** nthawi iliyonse akayamba kuchita chinthu chabwino, chothandiza, kapena chololedwa.

Akamaliza kuchita chinthu chabwino, chothandiza kapena chololedwa, anene kuti, "**Al-hamd-u-lillah.**"

Awonjezere kunena kuti, "**Inshaallah**," pamene akunena zoti zingachitike, mwachitsanzo, "Ndipita ku Liwonde …….".

Nthawi iliyonse akamva nkhani za chisoni anene kuti, **"Inna lillah wa inna ilaihi raji'un."**

Achite tawba ndi istighfar pamene akunena (kapena kuchita) cholakwika. Kuchita tawba ndiko kulapa tchimo linalake, kulisiya ndi kumulonjeza Allahu ta'âlâ kuti sadzabwerezanso tchimolo. Kuchita istighfar ndiko kunena kuti, "Astaghfirullah," ndipo potero kupempha chikhululuko kwa Allahu ta'âlâ.

Azinenanena Kalima tayyiba, **“La illaha ilallahu wahdahu la sharika lah, lahul-mulku wa lahul-hamdu wa huwa 'ala kulli shay'in qadir."**

Ayenera kunena Kalima sharifa pafupipafupi, **“Ash-hadu an La illaha ila Allahu wa ash-hadu anna Muhammadan ’abduhu wa Rasuluh.”**

Anene motere, usana ndi usiku:

1- **“Astaghfirullah”.**

2- **“Subhan-Allahi wa-l-hamd-u-lillahi wa la-ilaha il-lallahu wallahu akbar wa-la-hawla wa-la quwwata illa billah-il'aliy-yil 'adhim."**

MAKHALIDWE OTAMANDIKA (AKHLAQ HAMIDA)

Pali makhalidwe makumi asanu ndi awiri ndi mphambu ziwiri (72) omwe angawoneke okondeka pa munthu:

Iman; chikhulupiliro cha Ahl as-Sunnah; ikhlas; ihsan; tawadu’; dhikr-iminnat; nasihat; tasfiya; ghayrat; ghibta; sakha; isar; muruwat; fufuwat; hikmat, shukr; kuchotsaa; tsiku; khawf; raja; bughd-i-fillah; hubb-i-fillah; hamul; istiwa-i-dhem wa mad-h; mujahada; ayi; qasd; 'amala; dhikr-i-mawt; taf; taslim; talab-ul-’ilm; sala-'ahd; injaz-i-wa’d; husn-i-khulq; zuhd; qanaat; kuthamanga; sa’y-i-fi-l-khayrat; riqqat; sawq; ayia; thabat-i-fi amrillah; unsu billh; shawqu ila liqaillah; waqar; dhakawat; istiqamah; adab; firasat; tawakkul; sidq; murabata; musarata; muraqaba; muhasaba; muataba; kadhm-i-ghaydh; hubb-i-tul-i-hayahi li ’ibadatihi; tawba; khushu; yaqaan; 'ubudiyyat; mukat; ri’ayah-i-huquq-i-’ibad.

Tawadu’ ikutanthauza kudzichepetsa ndikukhala wa manayzi; dhikr minnat kutanthauza kudziwa kuti ntchito yomveral Allah ta’âlâ imafunika chiwongoko, thandizo ndi chifundo cha Allahu azeem ul shan ndi kuyamika kwa Allahu ta’âlâ pa zimenezo; nasihat ndiko kuchenjeza kapena kulangiza m'bale wako wa Mu’min (wokhulupirira);

tasfiya ndiko kuchotsa akhlaq-i-dhemima (mbiri za khalidwe loyipa) mu mtima mwako ndi kuukongoletsa ndi akhlaq-i-hamida (makhalidwe apamwamba); ghayrat ndi kupilira m’chikhulupiliro chako; ghibta ndiko kulakalaka utakhala ndi madalitso amene munthu wina ali nawo; sakha ndi futuwwat zonse zikutanthauza kuwolowa manja; isar ndiko kupeza njira zothetsera mavuto a abale ako omwe

ali Mu'min (okhulupirira); muruwwat ndiko kusenza udindo othandiza pa za umunthu; hikmat ndiko kudziwa 'ilm-i-hal (ziphunzitso za Chisilamu zokhudzana ndi ntchito zachipembedzo za Msilamu) ndi kugwiritsa ntchito zomwe ukuzidziwazo; shukr ndiko kugwiritsa ntchito madalitso pamalo ndi muchikhalidwe monga mmene Chisilamu chikunenera; rida ndi kusangalatsidwa ndi zomwe Allahu ta'âlâ anakukonzera; ndipo sabr ikutanthauza kuleza mtima ukakumana ndi zovuta.

[Ri'ayah-i-huquq-i-'ibad ndi kusamala ufulu wa akapolo a Allahu ta'âlâ, a anthu. Zofunika kwambiri mwa ufulu wa akapolo ndi ufulu wa kholo. Ndi mawu okoma ndi nkhope ya chimwemwe, tiyenera kuthamanga kukawathandiza ndi kuchita zonse zomwe tingathe kuti atikonde. Chotsatira ndi ufulu wa anthu oyandikana nawo, ufulu wa aphunzitsi athu, ufulu wa wokhala pa banja, ufulu wa anzathu, ndi ufulu wa boma lathu. Tisaname kwa aliyense kapena kuchita chinyengo kwa aliyense; tigwiritse ntchito zoyezera (ngati ma sikelo) zoyenera ndipo tilipire a ntchito athu thukuta lawo lisanaume. Ndi chiwembu kusabweza ngongole zathu kapena kusalipira pa ulendo watha wa pa basi kapena zina zotero. Kusakhoma misonkho ku boma ndi kulephera kuchitira chilungamo anthu miyandamiyanda. Tiyerekeze kuti boma likupondeleza anthu ndipo oponderezedwawo awukira boma, ndizosaloledwa kuthandiza owukirawo. Izi zalembedwa m'bukhu la **Bariqa,** pa mutu wa Fitna, komanso m'bukhu la **Fatawa Hindiyya** ndi **Durr-ul-mukhtar**. Kwanenedwanso mu Hadith sharif kuti: "**Ngati munthu achitira chinyengo Boma, Allahu subhanahu wa ta'âlâ adzamuchitiranso iye chinyengo,"** Allahu subhanahu wa ta'âlâ adzamuchepetsa wowukirayo ndi kumunyozetsa [Nibras]. Pa chifukwa ichi, tisapereke umboni ndi kufalitsa zosokoneza ndi zowononga zomwe zingachititse Asilamu kuwukira boma. Zinthu zolembedwa ndi anthu opanda Madhhab ena, monga **Sayyid Qutb** ndi **Mawdudi**. Kuwukira sichinthu chovomerezeka, ngakhale bomalo liri lopondereza, ndipo sikoyenera kuthandizira ogalukira. Ibni Abidin "rahima-hullâhu ta'âlâ", monga momwe akulongosolera, ndi haram kwa amuna kuvala zovala za silika, anati: "Ndi zololedwa kuyala nsalu za silika kapena kuonetsa zinthu za golide ndi siliva popanda kuzigwiritsira ntchito pa zikondwelero, monga, pa Eid ndi m'maukwati ndi cholinga chongokwaniritsa lamulo la boma osati mwamwano.

Koma kuwononga ndi kugwiritsa ntchito zinthu mopanda phindu ngati kuyatsa magetsi, kuyatsa makandulo kapena kuyika zowalitsa ndi zokongoletsa sikololedwa. Ndi zololedwa kutumiza ana anu ku sukulu

zosakanikirana anyamata ndi atsikana, ngati boma litalamula kuti anthu atero. Asilamu sakuloledwa kupita ku malo komwe amuna ndi akazi amasakanikirana ndipo komwe anthu amawonetsa ziwalo zawo za awrat. Zalembedwa mu **Ibni 'Abidin**, m'mitu yake yonena za 'swala ya la chisanu' ndi 'Kukhala Qadi', kuti ndikosaloledwa kugalukira ngakhale malamulo a osakhulupilira. Zanenedwa ndi akadaulo a Chisilamu kuti ntchito zopembedza zomwe zimaphwanya ufulu wa akapolo a Allahu ta'âlâ, sizidzalandiridwa ndipo sizidzathandiza wopembedza kulowa ku Mparadiso. Zanenedwanso kuti kulipira ufulu wa munthu yemwe si Msilamu ndi kovuta kuposa kulipira ufulu wa Msilamu. Timachita zabwino kwa aliyense koma tisachite chifundo kwa ochita zoyipa. Msilamu weniweni adzamvera malamulo a Allahu ta'âlâ ndi malamulo a boma.]

Gulu lodalitsika la Wali ndi lovuta kulipeza,
Anthu angalipeza sadzalisiya kuti lisokonezeke.

Munthu ayenera kuyang'ana kutali ndi pafupi kuti apeze munthu woyenelera;
Msintha ndalama amadziwa mwala wamtengo wapatali, osati Wopepera.

Msuko wotembenuza pansi pa mpope wa madzi;
udzakhala zaka makumi anayi, osatunga dontho la madzi.

Sohbat imayeretsa mtima, kuchititsa nsanje kumwamba;
Nzeru za munthu sizikhala pa chovala chokwera pachifuwa.

Yambani khalani ndi iman, ndi kusiya za haram;
Zomwe moyo umadya sizopaka zotsekemera pa nkate!

ZOKHUDZA ULEMELERO WAKU CHIPEMBEDZO WA MA SAHABAH

Mwa ma Sahabah onse a Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam", ma Khalifa anayi "radiyallâhu ta'âlâ 'anhum ajma'in" ndi amene ali apamwamba kwambiri. Nthawi ya ma Khalifa onse anayi inali zaka makumi atatu. [Ndi mfundo yachikhalire kuti Sahabah "radiyallâhu ta'âlâ 'anhum ajma'in" onse adzapita ku Mparadiso. Ndi kosaloledwa kunena zoyipa za aliyense waiwo.]

Keramat (kupambana) kwa Awliya ndi haqq (ndiko kuti ndi zoona).[1] Hadrat Abu Bakr as-Siddiq “radiyallâhu ta’âlâ ’anh” ndi wabwino kwambiri komanso wapamwamba kwambiri kuposa ma Wali onse (Awliya). Zoti anala khalifa ndi haqq (zoona). Zoti iye ndi Khalifa woyamba ndi zotsimikizika ndi ijma’ (kuvomerezana kwa Sahabah). Iye ndi mpongozi wa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”. Anakwatitsa mwana wake wa mkazi Aisha “radiyallâhu ’anha” kwa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”. Anali wodziwa bwino za Haqiqat. Anagwiritsa ntchito chuma chake chonse m’njira ya haqq, (njira ya chowonadi, Chisilamu) kotero kuti sanatsale ndi kalikonse. Choncho anavala zikhungwa za mtengo wa tende m’chiwuno mwake. Jebrail „alaihim-salâm” anavala chimodzimodzi ndikukamuchezera Mtumiki wa Allahu ta’âlâ. Pamene Mtumiki wodalitsika anawona Mngelo wamkuluyu atavala chovala chachilendo, anati: **“Ee, iwe Jebrail, m’bale wanga! Sindinakuwonepo chonchi chiyambire. Ndikudabwa kuti kodi chikuchitika ndi chiyani."** Pamenepo Jebrail „alaihim-salâm” anafotokoza kuti: “Ya Rasulullahu (Mtumiki wa Allahu ta’âlâ)! Tsopano ukundiwona nditavala chonchi. Angelo onse nawonso avala chomwechi. Chifukwa chake ndi ichi: Allahu subhanahu wa ta’âlâ anati: **‘Kapolo wanga Abu Bakr wapereka chuma chake chonse chifukwa cha chisomo Changa ndi njira yanga. Choncho amavala nyanda yopangidwa kuchokera ku mtengo wa tende. Ee, Angelo Anga. Inu valani ngati iye!’ Chotero angelo onse avala chonchi.”** Kuyambira pamenepo Hadrat Abu Bakr amatchedwa ‘Siddiq’ (ndi Allahu ta’âlâ komanso ndi Asilamu onse.)

Wali wachiwiri wabwino kwambiri ndi Hadrat Umar “radiyallâhu ’anh”. Ukhalifa wake ndi wowongoka molingana ndi ijma ummat (mgwirizano wa ma Sahabah). Iye amadziwa bwino za nthambi ya kudziwa.

Tsiku lina Munafiq[2] ndi m’yuda anabwera kwa Hadrat Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”. Iwo amadzamupempha Mtumiki

[1] Ndi ’adat-i-ilahiyya (chizolowezi choyera) cha Allahu ta’âlâ’s kulenga zinthu ndi zochitika pogwiritsa ntchito njira (sabab). Mwachitsanzo, chinthu cholemera kuposa madzi chimamira m'madzi. Nthawi zina Allahu ta’âlâamayimitsa lamulo Lake loperekera chisomo cha akapolo Ake okondedwa monga Atumiki ndi Awliya, kuti zochitika zomwe timazitcha zodabwitsa ndi zozizwitsa zichitike kudzera mwa anthu odalitsidwawa. Chodabwitsa chikachitika kudzera mwa Mtumiki ndi mu’jiza, ndipo chodabwitsa chimachitika kudzera mwa Wali (ambiri, Awliya) chimatchedwa keramat (Zambiril. keramat).

[2] Munafiq ndi kafiri amene amadzinamiza kuti ndi Msilamu, amakhala pakati pa Asilamu, nalowa nawo m’mapemphero awo ena omwe amawachitira limodzi (pa jama’at).

wodalitsika kuti aweruze mkangano pakati pawo. Hadrat Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anamva vuto lawo. Nkhani inakomera m’yuda, (choncho Mtumiki wodalitsika anapereka chigamulo mokomera m’yuda.) Pamene Munafiq sanakhutitsidwe ndi chigamulocho, Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”anati: “Anthu inu! Pitani kwa Umar ndipo muloleni kuti aweruze pakati panu!” Choncho anapita kwa Hadrat Umar “radiyallâhu ta’âlâ ’anh” . Pamene Sahabi wodalitsika anafunsa chifukwa chimene iwo anali kumeneko, munafiq anati: “m’yuda uyu ndi ine takhala tikukangana. Hadrat Umar “radiyallâhu ta’âlâ ’anh” adati: “Ndingaweruze bwanji mkanganowo monyoza Mwini Chisilamu (Mtumiki wa Allahu ta’âlâ)?” Munafiq anafotokoza kuti: “Tinapita kwa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”. Iye anapereka chiweruzo mokomera m’yuda. Ine sindinakhutitsidwe ndi kuweruza kwake.” Pomwepo Umar “radiyallâhu ’anh” anati: “Dikirani apa! Ndibweranso ndi yankho,” ndipo analowa m’nyumba. Patapita nthawi anatuluka ali ndi mpeni atabisa mu chovala chake, ndipo mosazengereza mutu wa Munafiq unadulidwa.

"Awa ndiye malipiro olungama kwa munthu amene sangavomereze chigamulo cha Rasulullah," anatero Sahabi wamkulu kufotokoza. Potengera nkhani imeneyi, iye anatchedwa Umar-ul-Faruq “radiyallâhu ta’âlâ ’anh”, ndipo wakhala akutchedwa choncho kuyambira pamenepo. Hadrat Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anati: **“Umar ndi amene amasiyanitsa chabwino ndi choyipa.”**

Wali wachitatu wabwino kwambiri pambuyo pa Umar ndi Uthman Zinnureyn “radiyallâhu ’anh”. Ukhalifa wake ndi woongoka, wolungama. Ndi chowonadi chotsimikizirika ndi ijma Ummat, (mgwirizano wa ma Sahabah.) Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anakwatitsa ana ake awiri odalitsika kwa iye, mmodzi pambuyo pa mnzake. Mwana wake wa chiŵiri atamwalira, iye anati: “**Ndikanakhala ndi mwana winanso wa mkazi, ndikanam’patsanso ameneyo.”** Pamene Mtumiki wodalitsika anakwatitsa mwana wake wa mkazi wachiwiri wodalitsika kwa ‘Uthman “radiyallâhu ta’âlâ ’anh”, anayamikira kwambiri mkamwini wake wodalitsika. Pambuyo pa tazwij (ukwati, chikwati), mwana wa mkazi wofunika kwambiriyo anati: “O, Atate wanga wokondeka! Munatamandira Hadrat Uthman kwambiri. Si wabwino Kwambiri koti mpaka ndikulandira matamando anu kotero.

Pamenepo Hadrat Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”anati kwa mwana wake wamkazi: **“Ee iwe mwana wanga wa mkazi! Angelo kumwamba ali ndi haya (manyazi) ndi Hadrat Uthman!”**

Chifukwa choti Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” anamupatsa Hadrat Uthman kukwatira ana ake akazi awiri, (wina atamwalira woyamba), iye amatchedwa Uthman Zinnureyn. Zinnureyn ikutanthauza mwini wa Nur ziwiri. Hadrat Uthman ndi odziwa bwino za ma’rifat (Chidziwitso chauzimu chokhudza chisomo cha Allahu ta’âlâ).

Wali wachinayi wabwino kwambiri pambuyo pa Hadrat Uthman ndi Ali ‘karrim-Allahu wajhah wa “radiyallâhu ’anh”. Ukhalifa wake ndi wolondola, mfundo yotsimikizika ndi ijma ummat. Iye ndi mpongozi wa Rasulullah. Mtumiki wokondeka wa Allahu ta’âlâ anampatsa iye mwana wake wa mkazi, Hadrat Fatima “radiyallâhu ’anha” kuti amukwatire. Iye ndi odziwa bwino za Tariqat. Iye anali ndi kapolo wamamuna. Tsiku lina kapolo wake anafuna kumuyesa mbuye wake. Hadrat Ali “radiyallâhu ta’âlâ ’anh” anali panja pa nthawiyo. Pamene analowa ndikupempha kapolo kuti amuchitire ntchito, kapoloyo anangokhala chete. Kenako Hadrat Ali ‘kerrem-Allahu wajhah’ anafunsa: “O iwe kapolo! Choyipa chanji chomwe ndakuchitira iwe ndipo ndi chiyani pa ine chomwe chakuwawa? Kapolo anayankha kuti: “Inu simunandilakwire kalikonse. Ine ndine kapolo wanu. Ndachita zimenezi kuti ndikuyeseni. Ndinu Wali weniweni."

[Asilamu amene amakonda Ashab Kiram (Sahabah) onse ndi kutsatira m’mapazi awo amatchedwa **Ahl Sunnah** (kapena **Asilamu a Sunni**). Amene akunena kuti amawakonda ena mwa iwo ndi kudana ndi ambiri mwa ma Sahabah amatchedwa ma Shia. Amene amadana ndi ma Sahabah onse amatchedwa ma **Rafidi.** Munthu amene akunena kuti amakonda ma Sahabah onse koma osatsata aliyense mwa iwo amatchedwa **Wahhabi**. **Wahhabi** ndi chipwirikiti cha maganizo a munthu wampatuko m’chipembedzo wotchedwa Ahmad ibni Taymiyya ndi mabodza a kazitape wa boma la Britain wotchedwa Hempher. Ampatuko amenewa amawatcha Asilamu a Ahl Sunnah kuti ndi ‘osakhulupilira’ chifukwa chakuti Asilamu enieniwo amakana ziphunzitso za chi Wahhabi. [Kuwasala komwe iwo amawasala Asilamu ena kumawabwelera iwo eni ndipo kumawachititsa iwo kukhala osakhulupilira.]

Ziphunzitso za Wahhabi zinayambitsidwa ndi achiwembu a ku Britain pa kachilumba ka Arabia mchaka cha 1150 [1737 AD]. Anakhetsa mwazi ochuluka wa Asilamu poyesetsa kufalitsa zofuna za

Angerezi. Makono akukhazikitsa malo a Wahhabi omwe amawatcha kuti **Rabita-t-ul alam-il-islami** m'dziko lirilonse ndi kumagonjetsa anthu osadziwa (osaphunzira) m'chipembedzo powapatsa ndalama ndi katundu. Kudzera m'njira izi akusocheretsa Asilamu ambiri. Iwo amanyoza akatswiri a Ahl Sunnah omwe akhala akuteteza Chisilamu kwa zaka zoposa 1400 ndi atetezi awo, a Ottoman.

Iwo akuti ziphunzitso zowona za Chisilamu za akatswiri odalisikawa zomwe ndi zochokera mu Nass (ayah ndi Hadith) ndi zabodza. Ena mwa ma Wahabi amati, "Ifenso tili mu Madhhab a Sunni. Ife tili mu Madhhab a Hanbali." Zonena zawozi ndi zofanana ndi zimene anthu a gulu la mpatuko lotchedwa Mu'tazila amanena, kuti, "Nafenso ndife Asilamu a Sunni. Ife tili mu Madhhab a Hanafi." Akutero chifukwa akudziwa kuti anthu amene sali m'gulu la Sunni adzapita ku Jahannama.

Zoona zake ndi zoti, kuyanjanitsa machitidwe a chipembedzo ndi kapembedzedwe ka gulu lina la anthu ndi amodzi mwa Madhhab anayiwo, sikutanthauza kuti anthu amenewo ali m'Madhhab amenewo. Kukhala mu Madhhab kumafunika kutsatira Madhhab amenewo m'chikhulupiliro ndi m'machitidwe. Madhhab onse anayi ndi ofanana m'zikhulupiliro zawo. Onse anayi ali m'njira ya Ahl Sunnah pa nkhani ya chikhulupiliro. Munthu kukhala m'Madhhab a Hanafi kapena Hanbali kumafunika kuti akhale ndi chikhulupiliro chogwirizana ndi (m'machitidwe) a Madhhab otchedwa Ahl Sunnah. Ma Wahhabi satsatira chikhulupiliro cha Sunni.]

CHAKUDYA NDI MADIBWE

Pali ubwino khumi wosamba m'manja musanadye pozindikira kuti kusamba m'manja ndi ntchito ya Sunnah:

Ngati munthu wasamba m'manja asanadye, ndi kuyendetsa zala zake (zolozera) zonyowazo, kuyambira kona ya mkati mwa diso kufikira pa kona yakunja, mogundisa zalazo mu zikope zake atatsinzina, munthu ameneyo, ndi chilolezo cha Allahu ta'âlâ, sadzadwala zilonda zo mmaso. Ubwino khumi wosamba mmanja ndi:

1- Mngelo yemwe ali mmunsi mwa Arsh-i-Rahman adzakupatsani malonje oyamikira: Chifukwa chosamba manja, machimo anu ang'ono ayeretsedwa.

2- Mudzalandira thawab ngati kuti mwachita Swalah ya nafila

3- Mudzatetezedwa ku umphawi

4- Mudzapeza thawab yolingana ndi imene yapatsidwa kwa Asidiq (munthu wonena zowona)

5- Angelo amamuchitira istighfar munthu wosamba mmanja (kumupemphera chikhululuko).

6- Pa mbali iliyonse ya chakudya chomwe akudya adzapeza thawab zochuluka ngati kuti wapereka sadaka ya chakudya chonsecho.

7- Adzayeretsedwa kumachimo ake ngati atayambanso kudya atanena mawu oti Bismillah.

8- Maduwa omwe anganene atatha kudya chakudya adzalandiridwa ndi Allahu ta'âlâ.

9- Ngati atamwalira usiku umenewo, adzapeza thawab yolingana ndi imene mashahidi (ofera chikhulupiriro) adapeza.

10- Akamwalira masana adzalembedwa m'gulu la mashahidi.

Kusamba m'manja ndi cholinga chochita ntchito ya Sunnah kuli ndi ubwino usanu ndi umodzi:

1- Mngelo yemwe ali mmunsi mwa Arsh Rahman adzati: "E, iwe okhulupilira! Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" wakondwera nawe."

2- Mudzapeza thawab zopatulika mwa padera chifukwa cha madalitso amenewa.

3- Thawab zomwe mudzapeza zidzakhala zochuluka ngati tsitsi la thupi lanu.

4- Mudzakhala ndi gawo lochokera ku nyanja ya Rahmat (Chifundo cha Allahu ta'âlâ).

5- Mupeza thawab zochuluka ngati kuchuluka kwa madontho omwe amagwa kuchokera m'manja mwanu.

6- Mudzamwalira ngati wofera mnjira ya Allahu ta'âlâ.

[Malamulo a Allahu ta'âlâ ali m'magulu awiri akuluakulu (Emr takwini ndi Emr tashrii)].

Amr takwini: Ndi kunena Kwake kuti, **"khala"** kwa zinthu zimene wafuna kulenga. Chinthu chimenecho chimakhalapo pamene Iye wati, "Khala!" Palibe amene angalepheretse chinthucho kukhalapo. Analenga zinthu zina kukhala gwero la zolengedwa zonse. Monga momwe wapangira zinthu zina kukhala gwelo la kulengedwa kwa zinthu zina, chimodzimodzi mphamvu za kuthupi ndi za uzimu za munthu komanso mitundu yosiyanasiyana ya mphamvu ndi gwero la kulengedwa kwa zinthu zina zambiri. Akafuna kupereka mphatso kapena chinthu chabwino kwa kapolo Wake, amampanga kapoloyo kupeza gwelo la mphatso imeneyo. Gwelolo likapezeka ndipo Iye ndikufuna nati 'khala!' chinthucho (mphatso, ndi zina zotero) chiyamba kukhalapo. Palibe chingakhale pokhapokha Iye atafuna.

Wabisa hikmah (upangiri) ndi kulengedwe Kake pozivindikira ndi magwelo. Anthu ambiri amawona ma gwelo okha koma kulephera kuona hikmah, Kulenga kwake kuseli kwa gwelo. Kusamvetsetsa kumeneku kumawapangitsa kuti awonongeke.

Amr tashrii: Awa ndi malamulo amene IYE wayika pa anthu okhudzana ndi zomwe ayenera kuchita ndi zomwe ayenera kupewa. Malamulo Akewa amadalira kufuna ndi kusankha kwa munthu. IYE wapereka ufulu kwa munthu kuchita chifuniro ndi chisankho chake. Komanso ndi IYE amalenga zinthu zomwe munthu amafuna ndi kusankha kuchita. Munthu akafuna ndi kusankha kuchita chinthu, Amachilenga ngati IYEnso wafuna. Salenga ngati sakufuna kuchilenga. IYE, yekha amalenga zinthu zonse ndi kupereka zinthu zogwira ntchito zosiyanasiyana. Palibe Mulengi wina pabali pa IYE. Kukhulupilira kuti pali wina pambali pa IYE amene ali ndi zizindikiro za Uluhiyyat (uMulungu) ndiko kumuphatikiza iye ndi zinthu zina. IYE walengeza kuti m'dziko liri nkudzalo sadzakhululukira aliyense amene akumuphatikiza IYE ndi chinthu china pa dziko lino. Ndipo adzapereka chilango chosatha ndi chowawa kwambiri kwa anthu ochita zimenezo. Anthu akasankha kutsatira lamula Lake ndi kuchita zabwino, Iye pokhala kuti ndi wachifundo, amafuna ndipo amalenga kumvera kwawo ndi ntchito zabwino Pomwe anthu okanira ndi kusamumvera akafuna kuchita zoyipa, Iyenso amafuna ndipo amalenga zoipa zawozo. Pomwe anthu amene amamukhulupirira akumupempha IYE kufuna kuchita choipa, pokhala wachifundo safuna choipacho ndipo salenga. Tsono chifukwa zofuna zoipa zonse za adani ake zimachitika kapena kukwaniritsidwa, iwo amagwera muzochita zoyipa kwambiri ndipo amakhala ponseponse kuononga.

Amr tashrii (malamulo) a Allahu ta'âlâ ali m'mageredi malinga ndi kufunika kwawo:

1- Walamula anthu onse kukhala ndi iman ndi kukhala Asilamu.

2- Walamula omwe ali ndi iman kuti asachite za haram gakhale uchimo.

3- Walamula omwe ali ndi iman kuchita zinthu Fardh.

4- Walamula Asilamu omwe amapewa za haram ndi kuchita ma Fardh kuti apewe makruh ndi kuchita Sunnah ndi ntchito zopembeza za nafila.

M'magawo ali pamwambawa, si chinthu chololedwa kusiya lamulo lofunika kwambiri ndi kuchita lamulo lomwe liri pa geredi ya pansi pake; sizokondedwa. Sizingakhale zothandiza. Ngati munthu apewa zoyipa popanda Iman kapena kuchita Fardh popanda kupewa uchimo

ndi haram kapena kuchita Sunnah ndi nafila popanda kuchita Fardh, Allahu ta'âlâ sangamukonde kapena kumuvomera zimene wachita.

Chomwechonso, ngati Msilamu sakuswali, sapereka zakat, sakulemekeza ufulu wa makolo ake kapena mkazi wake kapena ana ake, Allahu ta'âlâ sangamukonde kapena kumuvomera ntchito zake zabwino monga sadaka, zachifundo, zopereka, kumanga mizikiti, kuthandiza ndi ndalama kapena kusamba m'manja asanadye kapena akatha kudya komanso kapena kuchita Umra Tikhoza kuwona kuti aliyense ayenera kuchita awamir taklifiyya motsatira kufunikira komwe kwatchulidwa pamwambapa. Tiyerekeze kuti munthu wachita chinthu chocheperako popanda kuchita ntchito za pamwamba ndipo pakuteroko zamulepheretsa iye kuchita chinthu chomwe chiri fardh kapena zachititsa iye kusapewa haram; iye sakapeza thawab zilizonse, zomwe ziri zowona. Koma sikuti alephere kuchita ntchito yabwino imeneyo. Zalembedwa m'bukhu la Tafsir lotchedwa **Ruh-ul-beyan**, m'chigawo chomaliza cha mutu wa chisanu ndi chimodzi kuti, ndi baraka yopitilira kuchita zabwinozo, zikuyembekezeka kuti Allahu subhanahu wa ta'âlâ mwina mwachifundo angamudalitsa kuti athe kuchita malamulo a m'gulu lapamwamba.]

Pali fardh zinayi pa kudya:

1-Pomwe ukudya ndi kumwa, kudziwa kuti kukhutitsidwa ndi kukhuta kumaperekedwa kuchokera kwa Allahu adhim-ush-shan.

2- Idyani chakudya cha halal.

3- Kugwiritsa ntchito mphamvu zonse zomwe ukupeza kuchokera ku chakudyacho pochita ntchito yako ngati kapolo wa Allahu ta'âlâ.

4- Kukhala wokhutira ndi zomwe wapeza.

Pomwe mukuyamba kudya muyenera kuchita niyyah yanu kuti mukudya kuti mukhale ndi mphamvu yopembedza Allahu ta'âlâ, kuchita zinthu zothandiza akapolo a Allahu ta'âlâ, ndikuchichita chipembedzo cha Allahu ta'âlâ kukhala njira yopezera chisangalalo ndi mtendere osatha kufikira anthu onse. Ndikololedwa kudya osavala chirichonse pa mutu.

Mustahab pa kudya: Kuyika chonyamulira zakudya (cha matabwa) pansi (m'malo mwa tebulo lodyera); kuvala zovala za ukhondo pamene mukudya; kukhala pa mawondo anu; kusamba mmanja ndi mkamwa musanadye; kuchita Bismilla, ("Bismillah-ar-Rahman-ar-Rahim,") poyamba kudya; kulawa mchere pang'ono musanayambe kudya; kudya nkate wopangidwa ndi ufa wa bale; kutema nkate ndi manja; osataya zinyenyeswa za nkate; kudya mbali ya mbale yomwe ili pafupi ndi inu; kuyika ka viniga pang'ono; kudya nkate potema

tizidutswa ting'onoting'ono; kutafuna chakudya bwino; kudya ndi zala zitatu; kukombeza mkati mwa mbale ndi chala chanu; kunyambita zala zanu katatu; kuchita hamd mutatha kudya (kunena Al hamdulillah); kugwiritsa ntchito kamtengo kotokosera.

Makruh pa kudya: Kudya ndi dzanja la manzere; kununkhiza chakudya chomwe mukufuna kudya; kunyalanyaza kunena Bismillah; [Bismillah iyenera kunenedwa nthawi iriyonse ikakumbukiridwa, ngakhale mutatsala pang'ono kumaliza kudya.]

Haram pa kudya: Kupitiriza kudya utakhuta; [Ngati muli ndi mlendo, Yesetsani kupitiriza kudya kuwopera kuti mungamuletse kudya]; kuwononga chakudya; malinga ndi ena akatswiri, ndi haram kuchita Bisimillah pamene mukudya chakudya cha mwini wake popanda chilolezo; kuchita nawo phwando popanda kuyitanidwa; kudya chakudya cha munthu wina popanda chilolezo; kudya chinthu chomwe chingawononge thanzi lanu; kudya chakudya chokonzedwa ndi riya (mwamatama); kudya chimene unalumbira.

Kudya chakudya chotentha kwambiri kumayambitsa mavuto otsatirawa: Kugontha mkhutu; kutuwa nkhope; kusawala kwa maso; chikasu m'mano; kuti pakamwa pasamakhale bwino; kusakhutira; kufowoka mmazindikiridwe; kusokonekera malingaliro a munthu; zosayenera ku munthu.

Ubwino wodya pang'ono uli motere: Mudzakhala ndi thupi la mphamvu; mtima wanu udzadzazidwa ndi nur; mudzakhala okumbukira kwambiri; mudzakhala ndi moyo wofewa; mudzasangalala ndi ntchito zanu; Mudzakhala mutachita dhikr kwa Allahu adhim-ush-shan kwambiri; udzasinkhasinkha za tsiku lomaliza; mudzapeza kukoma kochuluka kuchokera mukulambira; mudzakhala ndi kuzindikira kozama ndi chiwongoko mu zinthu zonse; Mudzadutsa muchiweruzo chophweka (pa tsiku lachimaliziro)

Pamene munthu aliyense akunena: "Ine ndine Msilamu;
Tsiku lirilonse Swalah zisanu zalamulidwa pa iye.
Pa tsiku lakuwuka lomwe libwere posachedwa,
Zovala, nduwira ndi kavalo woti amunyamule.

UKWATI

Ukwati uli ndi zopindulitsa zambiri.

Choyamba, Ukwati umadzateteza chikhulupiriro cha munthu. Mudzapanga zizolowezi zokongola. Zopeza zanu zidzakhala ndi baraka.

Mudzakhala mutachita chinthu chomwe chili sunnat. Kunena zoona, Mtumiki wathu “sallallâhu alaihi wa sallam” anati: “**Pangani nikah**, (kwatirani popanga pangano la ukwati la Chisilamu lotchedwa ‘nikah’), **ndi kukhala ndi ana ambiri. Pakuti, pa tsiku la Kiyama ndidzanyadira mu kuchuluka kwa Ummah wanga** (Asilamu) **kuposa Ummah wa ena.**

Mamuna ayenera kulemekeza ufulu wa mkazi ndipo mkazi ayenera kulemekeze ufulu wa mamuna.

Munthu amene akufuna kukwatira afufuze bwino mpaka apeze mtsikana (kapena mkazi) amene ali Saliha (wokhazikika m’chikhulupiriro chake), yemwe si m’bale wake wa Mahram, ndipo akwatire mtsikana (kapena mkazi) amene akwaniritsa zomwe zakhazikitsidwa. Ndi kololedwa kupanga nikah ndi mkazi amene watenga mimba mwa chiwerewere. Ngati mimbayo wapatsidwa ndi mamuna wina, waty (kugonana) sikololedwa mpaka atabereka. (Fatawa Fayziyya).[1]

Musakwatire mtsikana chifukwa cha kukongola kwake kapena chuma chake. Mukatero mudzakhala onyozeka. Mtumiki wathu wodalitsika “sallallâhu alaihi wa sallam” anati: “**Munthu akakwatira mtsikana chifukwa cha chuma chake kapena kukongola kwake, adzalandidwa chuma chake ndi kukongola** kwake (kwa mkaziyo)**.”**

Ngati munthu akwatira mtsikana chifukwa cha kupembedza kwake ndi mbiri yake yokongola, Haqq ta’âlâ amamuonjezera katundu wake ndi kukongola kwake kwake (kwa mkaziyo).

Mkazi akhale wotsikirapo kwa mamuna wake mu zinthu zinayi: Zaka, msinkhu, anzake ndi abale ake. Mkazi ayenera kuposa mamuna wake pa zinthu zinayi: akhale wowoneka bwino komanso wowupeza mtima, wa makhalidwe abwino ndi wopewa za haram ndi zinthu zokayikitsa, asawonetse tsitsi lake, mutu, mikono ndi miyendo yake kwa amuna omwe ali na-mahram kwa iye.

Atsikana ang'ono sayenera kukwatiwa ndi amuna akulu. Zikhoza kuyambitsa fasad, (njiru.) Asanayambe zokhonzekera pangano la ukwati (nikah), mabanja a okwatiranawo ayenera kufufuza mozama za achinyamatawo, zomwe ndi sunnah ndipo zingathandize kulimbikisa ukwati.

Malinga ndi zonena za akatswiri a Chisilamu, izi zidzazetsa madalitso atatu: Choyamba, padzakhala chikondi pakati pa okwatirana moyo wonse; cha chiwiri, padzakhala baraka (yochuluka, kubereka

[1] Yolembedwa ndi Fayzullah Efendi waku Erzurum, Turkey “rahmatullâhi ta’âlâ ’alaih”(anaphedwa ku Edirne mu 1115 [1703 A.D.]), Ottoman Shaikh-ul-islam 46.

zipatso zodalitsika) m’ma rizq awo a moyo, chakudya cha tsiku ndi tsiku; ka chitatu, adzakhala atachita chinthu chomwe chili sunnah.

Zikatero, mwambo wovomerezeka wa ukwati m'delalo uyenera kutsatidwa. Ndi tchimo lalikulu kupanda kupanga (nikah) mogwirizana ndi Sunnah. Ndipo kudzakhala kulakwa kusamalizitsa mwambo wovomerezeka wa ukwati.

Nikah ikachitidwa molingana ndi Sunnat, banja la mamuna liyenera kutumiza mphatso zokongola ndi za mtengo wapatali kubanja la mtsikanayo; izi zimapititsa mtsogolo chikondi.

Ndikololedwa kwa mkazi kudzikongoletsa bwino kwa mamuna wake; Zimapereka thawab zambiri (malipiro a tsiku lomaliza).

Ndi sunnah kuchita phwando madzulo a tsiku la ukwati. [Chakudya chamadzulo chiyenera kudyedwa mutapemphera Swalah ya madzulo (Maghrb), ndipo mukaswali swalah ya usiku (Isha), mkwatibwi ayenera kutengedwa kupita ku malo a mkwati, ndipo pambuyo pa mapemphero olamulidwa ndi madalitso, gululo libalalike.

Mchitidwe wa sunnah wofunika kuchita usiku woyamba ndi woti mkwatibwi atsuke mapazi a mkwati ndi kuwaza madziwo kuzungulira nyumbayo. Mkwati aswali swalah ya rak’at awiri ndi kunena ma dua. Dua iliyonse yomwe idzapemphedwe mu usiku umenewo idzalandiridwa ndi Allahu ta’âlâ. Anthu amene amaona mkwati ayenera kumukumbutsa zimenezi. Anene kuti, **“Barakallahu lak wa barakaallahu 'alaiha wa jama'a baynakuma bi-l-khayri,"** kutanthauza kuti, "Allahu ta’âlâ akudalitseni nayo, ndipo adalitse mkazi wanu nayo, ndipo alumikize awirinu ndi khayr! (zabwino)." Pali anthu ena amayamikira banja la tsopano ponena kuti, “Mukhazikane bwino, mukhale ndi ana amuna ndi atchito!” Ndi mawu aumbuli ndi opanda nzeru. Ndi sunnah kunena pemphero loyenera pa nthawi yake.

Mamuna ayenera kudziwa ziphunzitso za chipembedzo zofunika ndi kuziphunzitsa mkazi wake. Ndithu, mudzafunsidwa za iwo tsiku Lomaliza. Kusadziwa sikungakhale chowiringula chovomerezeka. [Ndi fardh kuphunzira za fardh ndi za haram komanso ziphunzitso za chikhulupiriro cha Ahl sunnah ndi kuziphunzitsa kwa akazi ndi ana anu. Ndipo zili Sunnah kuphunzira ma sunnah ndi kuwaphunzitsa iwo.]

Musamtenge kapena kumutumiza mkazi wanu kumalo osaloledwa ndi Chisilamu! Musapite naye koyenda kapena kumulola kupita koyera osaphimba thupi lake bwino. Pakuti, Mtumiki wathu wodalitsika “sallallâhu alaihi wa sallam” ananena:

“Ngati mkazi afika pa mzikiti wathu atazithira mafuta onunkhilisa kuti kudzaswali, Swalah ya mkazi ameneyo sidzalandiridwa Allahu ta’âlâ, **pokhapokha atapita ku nyumba kukachita ghusl ngati akupanga ghusl ya janab.”** Popeza nkosaloledwa kwa iwo kupita ku mzikiti ndi fungo lokoma. Taganizira, ngati sikololedwa kupita ku mzikiti ndi fungo lokoma, lingakhale tchimo lalikulu bwanji kuzithira zonunkhilisa popita koyenda komwe ndi kokazionetsera kwa anthu. Tifananitse ndipo tiganizire kuti chilango chomwe adzalandire ndi chotani.

Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam” ananena mu imodzi mwa Hadith Sharif: **“Ambiri mwa anthu a ku Paradiso ndi anthu osauka (panthawi ya moyo wapadziko lapansi), ndipo ambiri mwa anthu a ku Jahannama ndi akazi** Pamenepo Hadrat Aisha “radiyallâhu ’anha” anafunsa: “Ndi chifukwa chiyani ku Jahannama kudzachuleke akazi?” Rasul karim “sallallâhu alaihi wa sallam” anafotokoza kuti: “**Saleza mtima tsoka likawagwera.** Samapirira vuto likawagwera. **Wina amene wakhala akuwachitira zabwino ndipo wachitira (tiyerekeze) zabwino khumi, kungowalakwira pang’ono nthawi zonse amatchula khalidwe loipalo, kuyiwaliratu zabwino khumizo. Amakonda zodzikongoletsera za padziko ndipo sagwira ntchito ya zozawathandiza tsiku Lomaliza ndipo amakonda miseche.**”

Anthu onse okhala ndi makhalidwe oipa ngati awa ndi anthu akumoto, amuna ndi akazi omwe.

Hadrat Ali karrim-Allahu wajhah akusimba kuti: “Tsiku lina mkazi wina anafika pamaso pa Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam” nati: “Ee Rasulallah! Ndikufuna kukwatiwa ndi mamuna. Maganizo anu odalitsika ndi otani?” Wodala wa Allahu ta’âlâ anayankha nati: **“Mamuna ali ndi ma ufulu ambiri pa mkazi wake. Kodi mudzatha kuzitsatira?”** Mkaziyo anati: “Ee Rasulallah! Ufulu wa mamuna ndi wotani?" **“Ukamulakwira ndiye kuti wawukira Allah, ndipo Swalah zako sizidzalandiridwa,”** linali yankho lochokera kwa wodalitsikayo. Mkaziyo anati: “Kodi pali ma ufulu ena?” **"Ngati mkazi apita kokayenda popanda chilolezo cha mamuna wake, sitepe iliyonse akuyenda ndi tchimo ndipo zimalembedwa (m'bukhu la ntchito zake),"** anayankha Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”. Mkaziyo anati: “Kodi alipo ena?” **“Ngati mkazi alankhulalira mamuna wake mawu oipa, pa tsiku Lachiweruzo mauwo adzapangisa lilime lake kutulukira kumbuyo kwa khosi lake,”** linali yankho lokongola kwambiri la Rasul akrim. Mkaziyo anati: “Kodi alipo ena?” **"Mkazi amene ali ndi chuma koma osatumikira zofuna za mamuna wake**

adzauka pa tsiku lomaliza ndi nkhope yakuda," anayankha Mtumiki wodalitsika.

Mkaziyo anafunsa kuti: "Kodi alipo ena?" Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" anayankha kuti: **"Ngati mkazi akuba ngakhale pang'ono chuma cha mamuna wake ndikuchipereka kwa wina, Allahu adhim-ush-shan sangalandire zakaat kapena sadaka ya mkaziyo pokhapokha atapempha chikhululuko kwa mamuna wake kuti amukhululukire ndipo mamunayo namukhululukira."** Mkaziyo anati: "Kodi alipo ena?" Kenako Mtumiki wodalitsika wa Allah anati: **"Ngati mkazi angatukwane mamuna wake kapena kukana kumumvera, iye adzapachikidwa ndi lilime lake m'dzenje la Jahannam. Ndipo ngati mkazi aliyense atuluka ndi kukaonera akazi akuvina ndi kumvera zida zoimbira ndi kulipirako kapena kufupako, twawab zonse zomwe adazipeza chifukwa cha ntchito zake zabwino kuchokera ku ubwana wake zidzathetsedwa. Zovala zomwe wavala ku malo a haramko zidzamusumira kuti 'Sanativale ife pa tsiku lopatulika kapena ali ndi mamuna wawo wa halal; Anandivala ku malo a haram komwe amapita.' Pamenepo Haqq ta'âlâ adzalengeza kuti: 'Akazi otere ndidzawatentha kwa zaka chikwi."** [Moteronso tiyenera kuzindikira kuipa kwa ma filimu ndi mapulogalamu a wailesi ndi wailesi yakanema.] MKaziyo atamva mayankho awa anati: "Ya Rasulallah! Sindinakwatiwepo chiyambire ndipo sindidzakwatiwa."

Nthawi yomweyo Rasul-akrim "sallallâhu alaihi wa sallam" mwa chisomo analongosola motere: **"Ya khatun** (Iwe mkazi)! **Ndiroleni kuti ndikudziwitseni za madalitso okwatiwa ndi mamuna; Tamverani! Ngati mamuna wa mkazi amuuza kuti, 'Allah akudalitseni ndi chisomo Chake,' zidzakhala zabwino kuposa kukhala wopembedza zaka makumi asanu ndi limodzi. Ndipo kumpatsa mamuna wake madzi akumwa ndi ntchito yabwino kwambiri kuposa kusala kudya kwa chaka chimodzi. Ngati achita ghusl pambuyo pa ntchito za kuchipinda ndi mamuna wake, adzapeza thawab yochuluka ngati kuti wachita Qur'ban. Ngati sachita chinyengo pa (mamuna wake) wa halal, angelo akumwamba adzapangira tasbih[1] m'malo mwake. Ngati acheza ndi kusewera mwachikondi ndi mamuna wake, adzakhala wodala kuposa kumasula akapolo makumi asanu ndi limodzi. Ngati ateteza rizq la mamuna wake ndi kuchitira chifundo anzake ndi bale a mamuna wake ndi kuswali kasanu pa tsiku ndi kusala kudya (mu**

[1] Kupanga tasbih kumatanthauza kunena kuti, "Subhan-Allah," kutanthauza kuti, "Ine ndikumudziwa Allah kuti ali kutali ndi zilema za mtundu uliwonse." Kupanga tasbih ku-mabweretsa thawab yochuluka (malipiro a tsiku Lomaliza).

Ramadan), n'kwabwino kuposa kukacheza ku Ka'ba kambirimbiri." Fatima Zehra "radiyallâhu 'anha" (Mwana wamkazi wodalitsika wa Rasulullah,) anafunsa kuti: "Chidzamuchitikira chani mkazi yemwe akunyoza mamuna wake wa Halal" Pamenepo wodalitsika kwambiri mwa abambo onse anati: **"Ngati mkazi wakana kumumvera mamuna wake, temberero la Mulungu lidzakhazikika pa iye kufikira atapempha mamuna wake kuti amukhululukire, ndipo mamunayo namukhululukira;**

Ngati mkazi akukana mamuna wake kuchipinda, adzataya thawab zake zonse;

Ngati azikweza pamaso pa mamuna wake, mkwiyo wa Allahu ta'âlâ udzakhala pa iye; ngati atanena kwa mamuna wake kuti, 'Kodi ndiwe ondiyang'anira?' kapena, 'Kodi unakhalapo wothandiza kwa ine?' Madalitso a Allahu ta'âlâ adzapanga haram kwa ine. Ngakhale atanyambita magazi a mamuna wake ndi lilime lake sakadzatha kulipira ufulu wa mamuna wake. Ngati mamuna wake amusiya kuti atuluke popanda kudziphimba bwino, machimo chikwi chimodzi adzalembedwa m'bukhu la zochita za mamuna wakeyo chifukwa chosamuzudzula." Zimenezi zidzathandiza kulongosola kukula kwa tchimo la mkazi chifukwa chongotuluka popanda chilolezo cha mamuna wake!

Rasul akrim "sallallâhu alaihi wa sallam" anati: **"Ya Fatima! Kukanakhala kuti Allah analamula zowumbidwa kuti azizigwadira zowumbidwa zina, ndikanalamula akazi kuti agwadire amuna awo."**

Hadrat Aisha "radiyallâhu 'anha" akusimba kuti: Ndinamupempha Rasulullah kuti asiye wasiyya kwa ine. Mtumiki wodalitsika adati:

"Ya Aisha! Ndisiya wasiyya kwa iwe ndipo upanga Wasiyya ndipo nawe upereke wasiyya umenewo kwa akazi a mu Umma wanga! Anthu akadzauka pa tsiku la chiweruzo: Mafunso adzayamba kufunsidwa za iman. Kachiwiri kudzafunzidwa za udhu ndi Swalah. Kwa akazi funso lachitatu lidzafunsidwa pa (ufulu wa) **amuna awo. Ngati mamuna apirira ndi kulankhula kwamnyozo kwa mkazi wake, Haqq ta'âlâ adzampatsa thawab yofanana ndi yomwe anapatsidwa Mtumiki Ayyub (Yobu). Ndipo ngati mkazi apirira ndi nkhanza za mamuna wake, Allah ta'âlâ adzamukweza mpaka kufika pa mlingo wa Aisha Siddiqa.**

Ngati mamuna amenya mkazi wake, ine ndi dzamudulira saman pa tsiku lachiweruzo," iyi ndi hadith ina yonenedwa ndi Rasul akrim "sallallâhu alaihi wa sallam".

Pali zifukwa zitatu zomwe mamuna amaloledwa kumenya mkazi wake ndi dzanja lake lotsegula kapena ndi mfundo ya kampango: Ngati atasiya Swalah, ngati asiya ghusl (kusamba), ngati akukana kubwera pa bed ya mamuna kapena kupita koyenda osazanzika. Ndi zosaloledwa ngakhale pang'ono kumenya mkazi ndi ndodo, chibagela matheche, mpango womanga mfundo kapena kumumenya pa mutu kapena pa thupi. Ndipo sayenera kumenyedwa chifukwa cha zolakwa zina. Ayenera kuchenjezedwa kangapo. Ngati athasintha, ndiye kuti ayenera kukhululukidwa kuopa kuzizunze.

[Zanenedwa motere mu **Shir'at-ul-Islam**: "Ngati mkazi wako ayamba kuonetsa khalidwe lotayirira, uzidzifunsa wekha. Mudziwuze nokha kuti, "Sakanachita chonchi ngati ndikanakhala wabwino. Ngati mkazi wako ali Saliha (oopa Mulungu), usatenge mkazi wachiwiri.

Ndi kosaloledwa kwa mamuna yemwe akuperewera kuchita chilungamo pa nkhani yosamalira banja lake, asakwatire mkazi wa chiwiri. Ngati akudziwa kuti angathe kuchita chilungamo, ndi nkololedwa kwa iye (kukwatira mkazi wachiwiri). Koma, ndi bwino kuti asatero. Mkazi wako akamapita kumalo komwe mwamuloleza kupitako, ayenera kufunda ku mutu ndi kuvala bwino thupi lake. Ndi haram kwa mkazi kutuluka atadzithira mafuta onunkhiritsa ndi kuonetsa zokongoletsa zake pa mtunda.

Mkazi wa Saliha (wopembedza) ndiye mdalitso wamtengo wapatali kwambiri wa padziko lapansi. Kuchitira chifundo ndi kukomera mtima Msilamu, kumabweretsa thawab yochuluka kuposa kupembedza nafila. Zalembedwa motere mu **Riyad-un-nasikhin:** ayah ya chikhumi ndi chisanu ndi chitatu (18) Sura Nisa ikunena kuti: **"Khalani bwino ndi akazi anu!**" Ma Hadith sharif otsatirawa: **"Ee Aba Bakr! Ngati munthu akulankhula akumwetulira, mwachikondi kwa mkazi wake, iye amapatsidwa thawab zochuluka ngati wamasula kapolo."** ndipo **"Mulungu sangachitire chifundo mkazi wokwatiwa ndi mamuna wa fasiq"** ndipo **"Amene akufuna shafa'at wanga asapereke mwana wake wa mkazi kwa mamuna wa fasiq kuti akhale mkazi wake."** ndipo **"**Wopambana mwa anthu ndi yemwe ali wabwino kwa anthu**. Munthu woyipitsitsa mwa anthu ndi amene amapezetsa mavuto anthu"** ndiponso **"Kupezetysa mavuto Msilamu popanda chilungamo n'koipa kuposa kugwetsa Ka'ba ka 70".**

Zanenedwa mu **Durr-ul-mukhtar** kuti: "Msilamu wa mamuna akakwatira mkazi ndikupanga naye nikah ndikhala mkazi wake, ndi chinthu cha fardh kwa iye kumusamalira pompatsa zofunika pa moyo wake zotchedwa nafaqa. **Nafaqa** zimakhala chakudya, zovala, ndi

nyumba. Ayenera kuonesetsa kuti mkazi wake akukhala m'nyumba yomwe ndi yake kapena imene wachita lendi. Mkazi angalamule kuti mchibale wa mamuna wake asaloledwe kuloŵa m'nyumba. Mamuna naye atha kulamula kuti wa chibale wa mkazi aliyense asalowe m'nyumbamo. Onse awiri ali ndi ufulu uwu. Nyumbayo ikhale ku mbali komwe kumakhala Asilamu a salih.

[Kukhale koti mawu a muazin akumveka popanda kugwiritsa ntchito zokulisa mau, popeza ndi bid'at kuigwiritsa ntchito zokulisa mau pochita za chisilamu.] Mamuna sangaletse mkazi wake kupita kokacheza ndi makolo ake kamodzi pa sabata. Akhozanso kubwera kudzacheza ndi mwana wawo wamkazi kamodzi pa sabata. Ngati mmodzi wa makolo a mkazi wadwala ndipo palibe wowasamalira, mkaziyo apite kukasamalira kholo lake ngakhale mamuna atamukaniza kutero.

Mamuna sangaletse achibale a mkazi ena omwe ali a Mahram kuzamuchezera, kapena kumuletsa kukawachezera kamodzi pa chaka. Ngati akumulola kuyendera abale ena omwe sa a mahram kwa iye kapena kupita kumalo omachimo, onse awiri adzakhala ochimwa. Amulese kuwagwirira ntchito anthu ena polandira malipiro kapena kwaulere, kunyumba kapena kwina kulikonse. Amulese kupita ku sukulu kapena kukalalikira. Mkazi ayenera kukhala wotanganika ndi ntchito za pakhomo pake; sayenera kumangokhala opanda chochita. Asamulole kupita koyenda kulikonse ndi anthu osavala zovala zowonetsa ziwalo, kumalo a anthu ambiri ngati kunyanja kapena kumalo kumene anthu amaonerako maseŵero. Sayenera kusunga wailesi yakanema m'nyumba mwake kuopera kuti zochita zoterozo zingawonedwe. Sayenera kuloledwa kutuluka atavala chovala chokongoletsera kapena chatsopano." Akhoza kumutengera ku malo komwe Asilamu opewa za haram amakhala, ngakhale atakhala kuti sali achibale ake a Mahram; koma kochezako amuna ndi akazi azikhala m'zipinda zosiyana. Amuna khumi ndi asanu ndi atatu (18) awa ndi omwe ali **Achibale a Mahram** a mkazi: Bambo ake ndi agogo ake; ana ake amuna ndi adzukulu zake amuna; azichimwene ake a bere limodzi, kapena abambo amodzi; ana amuna achimwene ake kapena chemwali ake; azimalume a kwa bambo ake ndi akwa mai ake. Amuna asanu ndi awiri awa ndi achibale ake a mahram ngati chibale chawo chili cha kubere kapena kudzera mchigololo. Ndipo amuna ena anayi akukhala achibale a Mahram pa njira ya Nikah (ukwati wolowa m'Chisilamu). Iwo ndi: Apongozi amuna ndi bambo awo; mkamwini; bambo wompeza; ana owapeza. Azipongozi amuna a mamuna wake komanso

azimuna a ana ake ndi abale awoa mahram. Wachibale wa Mahram amatanthauza munthu amene simungapange naye nikah (omwe simungamukwatire.) Mwachitsanzo, mamuna chemwali wake ndi mbale wake wa Mahram. Kwa mamuna, akazi a zichimwene ako, akazi a zimalume ake a kwa bambo ndi a kwa amayi ake, ana akazi azakhali ake, ana akazi a amalume ake a kwa bambo ndi a kwa mayi ake, amenewa si abale ake a mahram. Ana a mai ako akulu kapena ang'ono ndi amuna awo ndi na-mahram, (i.e. si achibale a mahram.) Azichimwene a mamuna wako kapena azichemwali a mkazi wako ndi na-mahram. Zoti mamuna wa mchemwali kapena mamuna wa a chemwali a mayi ake ndi azichimwene a mamuna wake ndi na-mahram kwa mkazi zalembedwa m'buku la Ni'mat-i-islam, pa mutu wonena za zofunika za Haji. Ndi haram kwa mkazi kudzionetsera kwa amuna amenewa popanda kudziphimba m'njira yophunzitsidwa ndi Chisilamu. Ndi haramnso kukhala nawo mwamseri m'chipinda chotseka ngakhale atadziphimba bwinobwino kapena kuyenda nawo ulendo wautali Safa).

Mtsikana sangakwatiwe ndi mmodzi mwa achibale ake a mahram. Ndi zololedwa kwa iye kukhala nawo popanda kudziphimba monga momwe amachitira pa maso pa amuna amene ali na-mahram kwa iye. Atha kukhala ndi mmodzi mwa achibale ake a mahram mwamseri mchipinda chotsekedwa kapena kuyenda naye ulendo wautali. Akafika wachibale amene si Mahram, amamuuza kuti: "Takulandirani," pa maso pa mamuna wake kapena akazi ena omwe ndi achibale ake koma thupi lake lonse litaphimbidwa kusiya nkhope yokha. Atha kuwakhonzera khofi, tiyi kapena zina zotero. Koma saloledwa kukhala pamenepo. Asilamu ayenera kutsatira mabuku ophunzitsa Chisilamu, osati miyambo ndi chikhalidwe. Msilamu aliyense ayenera kuphunzitsa mkazi wake Chisilamu ndi mfundo zothandiza. Ngati sanaphunzire bwino, amtumize kwa mkazi wamaphunziro okwanira ndi yemwe ali saliha (wowopa Mulungu) woti angamukhulupirire. Ngati sangapeze mkazi wotsatira Chisilamu ndi wopewa ma Haram, iye ndi mkazi wake akhale pamodzi ndikuwerenga mabuku ophunzitsa Chisilamu molondola ndi olembedwa ndi akatswiri a Ahl sunnat; potero onse awiri adzaphunzira Chisilamu, iman, za haram ndi fardh bwino lomwe. Asayipitse nyumba yake ndi mabuku a tafsir olembedwa ndi anthu achipembedzo osatsatira Madhhab alowonse; mabuku oterowo sayenera kuwerengedwa. Mnyumba musatseguliodwe ma wailesi ndi ma kanema okhala ndi ma pologalamu owononga Chisilamu komanso owonetsa makhalide oyipa. Zinthu izi ndi zoyipa kuposa magulu a anthu oyipa.

Zidzawononga chikhulupiriro ndi makhalidwe abwino a mkazi ndi ana anu. Akazi ndi ana akazi ayenera kukhala otanganidwa ndi ntchito za pakhomo; sayenera kugwira ntchito m'minda, m'mafakitale, m'mabanki, m'makampani kapena ntchito za boma. Sikofunika mkazi ndi ana akazi kuthandiza amuna ndi abambo awo pa zomangamanga ndi malonda. Ndi udindo wa mamuna kugwira ntchito za pakhomo zimenezi. Ndi udindo wa mamuna kukagula zofunika pakhomo m'masitolo ndi m'misika ndi kuzibweretsa kunyumba. Ngati mkaziyo akakamizidwa kuchita ntchito izi, chikhulupiriro chake, kalidwe lake ndi thanzi lake zidzawononge ka. Moyo wa dziko lino ndi wa dziko lili mkadza wa awiriwo udzaonongeka. Adzakhala achisoni, koma osapindula. Poti khalidwe ili silidzawapulumutsa iwo ku machimo ndi masoka. Munthu amene akumvera Chisilamu adzapeza mtendere pa dziko lapansi ndi tsiku lomaliza. Tidzisinthe tokha ndikutsatira mabuku otiphunzitsa za chipembedzo chathu. Tisatengeke ndi kumwetulira ndi mau achiphamaso a anthu otchedwa ma munafiq. Titeteze ana athu akazi ndi amuna ku za haram. Titumize ana athu ku sukulu zomwe ziri ndi aphunzitsi achisilamu. Mkazi sayenera kugwira ntchito pakati pa amuna m'masitolo, m'mashopu, m'mafakitale kapena ntchito za boma. Ngati alibe mamuna, kapena ngati ali ndi mamuna wosathekera, abale a mahram a mkaziyo ayenera kupereka zosowa zake zonse.

Ngati abale akewo ali osauka, ndiye kuti Boma liyenera kumupatsa ndalama zokwanira. Allahu ta'âlâ waika zosowa zonse za mkazi pafupi ndi iye. IYE amaika udindi wosamala moyo wa mkazi pa mamuna. Ngakhale kuti mkazi safunikira kugwira ntchito kuti apeze zofunika pa moyo, IYE amampatsa mkazi theka la gawo la chuma cha mamuna ngati chuma cha otsala. Ntchito za mkazi zimakhala ntchito za pakhomo. Choyamba ndi chofunika kwambiri mwa ntchito zimenezi ndi kulera ana. Murshid (Mtsogoleri) woyamba wa mwana ndi mayi ake. Mwana akaphunzira za chipembedzo ndi makhalidwe abwino kuchokera kwa amayi ake, sangasocheretsedwe ndi aphunzitsi osapembedza, ndi magulu oipa, kapena mabodza a zindiq omwe ndi adani a Islam. Amakhala Msilamu weniweni monga makolo ake. Ma munafiq amene amachita zoipa zotsutsana ndi Chisilamu amatchedwa zindiq.]

KUSAMBISA, KUVEKA NDI KUYIKA MSILAMU WAKUFA (TAJHIZ, TAKFIN NDI TADFIN YA JANAZA)

Kuswalira Msilamu wakufa, kusambitsa, kuveka ndi kuyika mmanda Msilamu wakufa, zonsezi ndi ntchito za farz.

Posambitsa mtembo wa Msilamu wakufa, mtembowo umagonekedwa chagada pa cement kapena benchi ya matabwa yoyikidwa polimba. Malaya amavulidwa. Mtembowo mumawupangisa udhu. Kumtunda kwa thupi lake, kuchokera ku mutu mpaka pa mchombo, umasambitsidwa ndi madzi ofunda. Gawo lake lapakati kuyambira pa mchombo mpaka m'mawondo limafundisidwa ndi kusambitsidwa. Munthu wosambitsa amavala magolovesi m'manja. Amalowetsa dzanja (lovala gulovu) mkati mwa chofunditsacho ndi kuthira madzi ndikutsuka gawolo (lophimbalo). Asayang'ane mbali ya thupi lofunditsidwalo. Kenako mtembowo amautembenuzira kumanzere ndipo mbali yake yakumanja imasambitsidwa; Pambuyo pake amatembenuzira kumanja, ndipo mbali yake yakumanzere imasambitsidwa. Imodzi mwa magawo atatu a nsalu yosambitsira imayaladwa pa benchi ndi pansi pa mtembo. Kenako nsalu yoyalidwayo ndi mtembo zimayikidwa chitanda.

Nsalu (kafan kapena sanda) zilipo mitundu itatu: Kafan farz, [yomwe imatchedwanso kafan darurat;] kafan sunnat; ndi kafan kifaya.

Kafan sunnat ya mamuna imakhala ndi magawo atatu, ndipo ya mkazi imakhala ndi magawo asanu.

Kafan kifaya ya amuna imakhala ndi magawo awiri ndipo ya mkazi imakhala ndi magawo atatu.

Zanenedwa mu **Bahr-ur-raiq** kuti: Kafan kifaya ya mkazi ndi izar, lifafa ndi himar (chomwe ndi chovala ku mutu). Poti akazi amayesetsa kufunda zidutswa zitatu zimenezi ali ndi moyo." M'masiku akale, Izar chinali chovala chophimba thupi lonse kuyambira mmapewa kapena kuchokera ku mwamba mpaka kumapazi. Zoti lifafa ndi qamis (dilesi longovalidwa popachika mmaphewa) zolembedwa ndi Ibni Abidin. Monga zikuonekera, akazi kale ankavala chibulandi ndi chipewa kumutu akamapita koyenda. Kwalembedwa **mu Bahr-ur-raiq** ndi **Dur-ul-muntaqa** kuti: "Nafaqa yomwe ili wajib kwa mamuna kumpezera mkazi wake ndi chakudya, zovala ndi nyumba. Zovala ziyenera kukhala himar (chovala kumutu), milhafa -chovala chakunja, [masiku ano chimatchedwa 'faraja' kapena 'manto' kapena 'saya'. Monga

tikuonera, chovala cha mkazi chimakhala ndi zidutswa zitatu, ndipo charshaf si chimodzi mwa zidutswazi.

Charshaf inalowa mu fashoni pambuyo pake. Ndi zololedwa kwa akazi kuvala charshaf ku malo komwe kuvala charshaf ndi chikhalidwe chake. Ndipo avale malaya otaya bwino ndi chovala chakumutu kumalo komwe amavala choncho mwa chizolowezi. Kuvala mozipatula ndi mosiyana ndi ena mdelalo kuzaetsa fitna, yomwenso ndi haram.]

Kafan[1] farz imakhala chidutswa chimodzi kwa amamuna ngakhale mkazi.

Kumalo komwe kulibe nsalu kupatula silika, chidutswa chimodzi kwa mamuna ndi kwa akazi zimafunika ziwiri. Imam woyenera kutsogolera Swalah ya janaza ali motere: Purezidenti, ngati ali Msilamu; woweruza milandu wa mu mzindawo; khatib yemwe wavomerezedwa kutsogolera swalah ya la Chisano ndi imam-i-hay.

Munthu wotchedwa imam-i-hay ndi Msilamu wophunzira bwino yemwe Msilamu womwalirayo ankakonda kumuyamikira ndi kukhala naye maganizo abwino pamene iye anali ndi moyo.

Wotsatira mundondomeko imeneyi ndi wali wa malemuyo. Ngati wali palibe ndipo Swalah yatsogoleredwa ndi Msilamu yemwe si m'modzi mwa anthu omwe tawatchulawa, wali adzakhala ndi mwayi wosankha. Atha kubwereza swalayo kapena ayi.

Tiyerekeze kuti munthu wadulidwa pakati (mulitali) ndipo theka limodzi la mtembo lapezeka, Swalah ya janaza sayingachitike ndi theka lokhalo. Tiyerekeze mtembo wong'ambika ndipo zidutswa zake zili apa ndi apo; Swalah ya janaza siyingachitike. Koma, Swalah iyenera kuchitidwa ngati zidutswazo zasonkhanitsidwa pamodzi.

Ngati mtembo wasambitsidwa koma akunena kuti chiwalo chimodzi chauma; chiwalocho chiyenera kusambisidwa ngati mtembo sunavekedwe. Tiyerekeze kuti, Janaza yafika kumanda ndipo kwadziwika kuti chiwalo chimodzi chofunika udhu chasiyidwa chouma; chiwalocho chisambitsidwe ndipo swalah ya janaza ichitikenso. Kudziwikako kukachitika mtembo utalowa mmanda, mtembo udzatulutsidwe. Ngati kwapezeka kuti mtembo siunasambitsidwe koma walowa kale mmanda, pamenepo mtembowo udzatulutsidwe ndikusambitsidwa ngati kukwilira kunali kusanachitike.

Tiyerekeze kuti mwasambitsa mtembowo mnjira ya tayammamu, kenako ndi kupeza madzi monga momwe mukunyamula mtembowo;

[1] Tanthauzo la lexical la kefen (kapena kafan) ndi 'nsanda'.

muli ndi ufulu wosankha. Tiyerekeze kuti anthu angapo amwalira nthawi imodzi m'tauni; ndi zololedwa kwaswalira swalah ya Janaza imodzi onse. Koma ziyenera kuchitika mogwirizana ndi malamulo a Chisilamu. Koma ndi bwino kuchita Swalah ya aliyense payekhapayekha.

Niyyat ya Swalah ya janaza iyenera kupangidwa motere: "Ndikupanga niyyat yanga **kuchita Swalah mwa chisomo cha Allahu ta'âlâ, kulemekeza Msilamu wamamuna** [kapena wamkazi], **ndi kutsatira imam yemwe akutsogolera Swalah yi."**

Tiyerekeze kuti munthu wamangidwa akubera alendo ndipo waphedwa ndi potsatira chiweluzo cha oweruza kapena ndi wali; kapena owukira boma waphedwa akumenyana ndi boma; kapena munthu waphedwa chifukwa chopha makolo ake; Swalah ya janaza siyimachitika kwa anthu atatu awa.

Swalah ya janaza imachitidwa ngati munthu wadzipha yekha (**Durr-ul-mukhtar**).

Asilamu a Sunni ali ndi ziziwitso khumi:

1– Msilamu wa Sunni amapita ku mzikiti nthawi zonse kukachita Swalah mu jamaat.

2- Amaswali mu Jama'at ndikuchita motsogozedwa ndi imam yemwe chikhulupiriro chake ndi fisq (machimo) sizili zoipa mpaka kumupanga kukhala kafiri.

3– Amavomera za kuloledwa kupanga masah pa ma masts.

4– Sadzanena zoipa za Ashab kirim "radiyallâhu ta'âlâ 'anh ajma'in " aliyense.

5- Sadzaukira boma.

6- Sadzalimbana kapena kukangana pa nkhani ya chipembezo popanda chifukwa.

7- Sadzakhala ndi chikaiko pa chipembedzo.

8- Amadziwa kuti chilichonse, chabwino kapena choipa, zimachokera kwa Allah Ta'âlâ.

9- Sadzanena Msilamu aliyense mwa anthu a ku Qibla kuti kafiri [pokhapokha ngati ihad yawo itadziwika].

10- Iye adzaika patsogolo ma Khalifa anayi (oyambirira) kuposa ma Sahabi ena.

MITUNDU YA IMFA

Anthu omvetsa chisoni ndi ofowoka inu! Mukuthawa imfa? "Wakuti wakuti afa. Ndikakhala naye pafupi akandipatsira," mukutero.

Muliri kapena matenda ena oopsa opatsirana akafalikira ku dera lina, mumathawira kwina. Ndi haram kukhala ndi chikhulupiriro choterocho. Matenda adzakugwerani ngati Allah atafuna.

Anthu omvetsa chisoni ndi ofowoka inu! Mukuthawira kumalo ati? Imfa ndi mapeto amene mudalonjezedwa. Imfa siidzachedwetsedwa ngakhale kwa mphindi imodzi! Nthawi yanu ya imfa ikakwana, Khallaq alam (Mlengi wa zolengedwa zonse) sadzakulolani kupuma ngakhale nthawi yapang'ono ngati kuphetira. Imfa siyizachedwetsedwa kapena kufulumizidwa, idzafika pa nthawi yake inakhazikidwa.

Kulikonse komwe Haqq ta'âlâ anamulembera munthu kuti adzafera, munthu adzakapezeka kumeneko, kusiya chuma chake chonse, banja lake ndi ana ake. Ndipo mzimu wake suwudzatulutsidwa mwa iye pokhapokha atafika pamalo pomwe nthaka yake ikumuyembekezera.

Aliyense adzafa nthawi ya imfa yake ikakwana. ayati karima 34 Sura ya A'raf imati: "... Ndipo nthawi yawo ikadza sangachedwe ngakhale ola limodzi, ndiponso sangaitsogolere".

Munthu asanabadwe, zimakonzedweratu kuti adzakhala ndi moyo wautali bwanji. Ndipo zonse zimakhala zitalembedwa mu Lawh mahfuz: komwe munthuyo adzafere, ngati adzafa atapanga tawba kapena ayi, ndi matenda ati amene adzafe nawo (ngati alipo), kuti adzafa ndi iman kapena ayi. Ndipo mfundo imeneyi yalongosoledwa mu ayah yomaliza ya Sura Luqman.

Khallaq alam adalenga imfa. Ndi kuzalenga moyo. Kenako analenga rizq lathu ndikuzilemba mu Lawh mahfuz.

Haqq ta'âlâ amadziwa kuchuluka kwa mpweya womwe muyenera kupuma. Ndipo anazilemba m'bukhu la Lawh mahfuz. Angelo amasunga bukhuli ndipo nthawi ikakwana amamudziwitsa Malaka-ul-mawt (Mngelo wa imfa).

Ngati mwakhala mukukhulupirira zomwe zanenedwa m' Qur'an al-kareem ndikuchita malamulo omwe anenedwa m'menemo, mudzapita ku dziko lotsatira ndi chisangalalo! Khulupirirani kuti chilichonse chikuchokera kwa Allahu ta'âlâ! Musalire modandaula kuti munthu wafa inu muvutika. Mchitidwe uwu umapangitsa munthu kufa opanda iman. Tithawire kwa Allah taala. Tikachimwa kapena kulakwa tiyenera kuchita tawba-i-nasuh.

Haqq subhanallahu wa ta'âlâ akulamula Azrail "alaihim-salâm" (Mngelo wa imfa) kuti: "Chotsani miyoyo ya anzanga mwachikondi

ndipo miyoyo ya adani Anga mwaukali!" Al-ayaz-u-billah, ngati munthu atakhala wosamvera!

Mmoyo ulimkudza, tsiku lomodzi ndi lalitali ngati zaka chikwi chimodzi kapena makumi asanu. Pali mafotokozedwe osiyanasiyana okhudza nkhaniyi. Mfundo iyi ikumveka kuchokera mu ayah karima ya chisanu mu Sura Sajda (32) komanso kuchokera mu ayati karima ya chinayi mu Sura Ma'arij (70).

Kenako Angelo amachotsa mzimu wa munthu wosamverayo mozunza. Mazunzo ake ndi osasimbika. Tikukhulupirira mwa Allah yemwe anatilenga kuchokera popanda kanthu. Anthu ena pa kufa amavutika, kutembenukira uku ndi uku. Zoona zake zafotokozedwa ndi Allahu ta'âlâ mu Sura Naziat (79). Angelo anawazunza mwa nkhanza, ndipo tsopano amayankhula wina ndi mzake. Jebrail "alaihim-salâm" akuti kwa iwo: "Musamchitire chifundo!" Mzimu wa munafiq umafika pa mphuno pake. Kenako angelo amausiya. Amamufinya mwa mphamvu ziwalo zake zonse kotero kuti kuwala kwa maso ake kumagwa. Angelo amamuuza kuti: "Iwe si wa ku m'Paradiso!

Kodi waiwala zoipa zimene umachita mu nthawi imene unali moyo? O iwe munthu wopanda pake! Chilango chakonzedwe kwa iwe ndi chilango cha ma munafiq ndi osakhulupirira. Poti munalibe nazo ntchito za Swalah, Zakaat, Zopereka, kapena zokuchitira chifundo osauka. Simundapewe zoipa, ndipo zochita zanu zonse zinali za fasad (zakatangale). Mumachita miseche ndikumati: 'Allah ndi wachifunda.' Tsopano chilango chako ndi mazunzo owawa." Kenako Hadrat Haqq subhanahu wata'âlâ akulankhula kuti: "Ma munafiq amenewo sanaganizire za imfa yawo ngakhale tsiku limodzi. Iwo anali odzikuza. Samapanga za fardh, sunnat, kapena wajib. Choncho aone mazunzo anga tsopano!" Apanso ma Zabani (Angelo a zizunzo) adzagwira matako ake ndi zikhadabo zake ndi kukoka mzimu wake kudzera m'mitsempha ya pa chifuwa chake, ndikuutenga kudzera pa kholinga lake kenako ndi kuutsitsanso. Apanso, mawu ena (ochokera kwa Allahu ta'âlâ) akubwera, akuti: "Kodi akatswiri achipembezo sanakuuze? Kodi siunawerenge Bukhu Lathu? Kodi silinanene: ifa isakupezeni modzidzimutsa (usanakhonzeke), ndipo usatsatire Mdyerekezi? Kodi salinanene kuti: "Chilichonse ndi chochokera kwa Allah?" Osadandaula za dziko lino, malo a mitembo! Khutirani ndi zomwe wakupatsani Allahu ta'âlâ, achitireni chifundo akapolo Ake osauka, ndipo dyetsani masikini.

Allahu ta'âlâ ndi wozidalira moti anakulengani ndi kuonetsetsa kuti akudyetseni, ndipo tsoka kapena vuto lochokera kwa Iye likakugwerani funsani ndi kumpempha Iye ndipo mpemphaninso chipulumutso. Musanene kuti, 'Ndalipira madokotala ndipo andichiritsa!' Dziwani kuti Allahu ta'âlâ ndi Yemwe wakupulumutsani! Chuma chomwe mumati ndi chanu ndi wongokusungitsani kuti mumsamale. Chuma ichi sichingakuchiritseni ku zowawa zanu. Ngati chapezedwa mwa m'njira ya Halal, mudzawerengetseredwa. Kanthu kalikonse komene Haqq subhanehu-wa-ta'âlâ wakulamulirani, mudzachilandira; sikudzakhala thandizo lochokera ku chuma chako, kwa ana ako, kapena kwa abwenzi ako. Ndipo simudzathawa mapeto ako, ngakhale utalira mochuluka bwanji; ngakale utathawira kuchipululu kwina kulikonse. Mapeto ake udzaikidwa m'manda pamalo pomwe pali nthaka yomwe unakhonzedwera kudzakhala manda ako. Ngati nthawi ya imfa yako siyinakwane, palibe angakuphe. Koma mwalamulidwa kuti mudziteteze ku zoopsa ndi kutsatira zomwe zingakupewetseni ku mavuto.

Ndipo nthawi iliyonse Haqq ta'âlâ akakupatsani madalitso monga thanzi, chuma ndi ana, mumakondwera nazo ndi kunena: "Mbuye wathu watichitira chifundo." Koma pamene Allah ta'âlâ akupatsani chinthu chowononga, akakutumizirani tsoka, mumakhumudwa mmalo mopirira ndi kuiwala kuyamika.

Liwu lochokera kwa Haqq ta'âlâ likunena kuti: "E, inu angelo Anga! Mgwireni!" Angelo amagwira mzimu wake kuchokera pansi pa tsitsi lake lonse, ndikumusiyanso.

Palibe amene ali ndi mphamvu zopulumutsa munthu amene akuzunzidwa ndi Allahu ta'âlâ.

Pa nthawi ya imfa munthu akawona mazunzowa amadandaula nati: Kalanga ine! Ndikulakalaka ndikanagwira ntchito zolamulidwa za chisilamu pomwe ndinali pa dziko, motero sindikanazumzika ndi mazumzo ndikuwawonawa. Pamenepo liwu lochokera kwa Allah likunena kwa anthu amene amayang'anira ovutika: "E, inu akapolo Anga odzitukumula! Tiyeni mpulumutseni mnzanu uyu pogwiritsa ntchito chuma chanu! M'dziko lapansi simupirira ndi masoka ochokera kwa Ine, ndipo simudandaula za Ine. Pano, kapolo uyu ali m'mazunzo ndipo mzimu wake wafika pa kholongo pake. Ndi Mphamvu Zanga!" Angelo akamva liwu ili amagwada pansi nati: "E, Mbuye wathu! Chilango chanu ndi Haqq (choona, cholondola)!" Haqq ta'âlâ akutidziwitsa za zochitika izi mu Qur'an al-kareem.

Pambuyo pake, mawu ena amabwera kuuza angelo kuti “Mgwireni.” Kugwira kwawo kumakhala kowawa kwambiri kotero kuti palibe muzu wa tsitsi la thupi lake lomwe silimamva kuzunzikako. Angero amafuula pamodzi nati: “E, iwe mzimu wa kapolo wa Allah wonyoza! Bwera ndipo tuluka m'thupi lakoli. Lero ndi tsiku la chilango kwa iwe chifukwa unali kukonda zolengedwa zina kusiya Allah; unali kudzikuza popereka moni kwa osauka; unali kuchita zinthu za haram; zoyipa umaziona ngati zolungama, ndipo zolungama ngati zolakwika.” Izi zafotokozedwa mu Qur’an al-kareem.

Ndipotu munthuyo amapempha kwa angelo kuti: “Ndiloleni kuti ndipumeko kwa kamphindi kuti ndidzitolere. Pamenepo akuwona Mngelo wa imfa atayima pambali pa kama lake. Akangomuona Mngelo wa imfa iye amayamba kunjenjemera, kuyiwala za mazunzo amene wakumana nawo aja. Akaona Mngelo wa imfa anena kuti: “Ndi Iwe ndani ukupezeka pomwe ndikuzunzidwa ndi angelo onsewa, ndipo uli pano chifukwa chiyani? Pamenepo imfa idzagwa ndi mantha onse amene imabwera nawo: Ine ndine imfa imene idzakuchotsani pa dziko la pansi, ndikusandutsa ana anu kukhala amasiye ndi kulola achibale ake osakadza kutenga chuma chako.

Akamva mawu amenewa kuchokera ku imfa, amanjenjemera ndi kuthawitsa nkope yake potembenukira mbali yina. Poti ichi ndi chizindikiro chomwe Rasululla “sallallâhu alaihi wa sallam” analozera mu Hadith sharif yolembedwa mu Sahih Bukhari: “Akamva angelo, atembenuzira nkhope yake kukhoma, naona imfa yaima pamaso pake”.

Kulikonse kumene akutembenukira amaona imfa pomwepo, kenako amatembenukanso kumbuyo kachiwiri.

Mngelo wa imfa akufuula mwamphamvu kuti: “Ine ndine mngelo wamkulu uja amene ndinachotsa mizimu ya makolo ako; iwe unalipo koma unawathandiza chotani? Tsopano abale ako onse akuwona iwe ukuvutika. Koma ali ndi phindu lanji? Ine ndine mngelo wamkulu uja, ndipo anthu amene ndinawapha pamaso pako anali ndi mphamvu zambiri kuposa iwe.

Pamene munthuyu wagona pa kama ndi kumayankhula ndi angelo, angelo ozunza amasuntha ndi kuchoka. Iye akaona Azrail “alaihim-salâm” (Mngelo wa imfa) ndi maonekedwe ake ochititsa mantha a mngeloyo, maganizo ake amasokonekera pa nthawi yomweyo.

Azrail “alaihim-salâm” amafunsa kuti: Kodi munalipeza bwanji dziko? Iye amayankha: Ndinachita zachinyengo za dziko ndipo zotsatira za kudzikonda kwanga ndi zimenezi.

Ndipo Khallaq jihan (Mlengi wa zolengedwa zonse) amasintha dziko kukhala mkazi. Ndi maso ake owopsa amtundu wakumwamba, mano ake ngati nyanga za ng'ombe ya mphongo, ndi fungo lake loipa. Mkazi ameneyu amakhala pachifuwa chake.

Nipo amamubweretsera chuma chake. Ngakhale iye akudandaula amapereka chuma chake chomwe anachipeza posalabadira kuti chinali cha halal kapena haram, kwa olowa m'malo mwake.

Kenako chuma cha munthuyo chimayankhula. 'O iwe kapolo wosamvera! Unandipeza ine ndikundigwiritsira ntchito mnjira zopanda chilungamo. Siumalipira zakah ndipo siumapereka sadaka. Pano sindilinso mmanja mwako ndipo ine ndi chuma cha anthu omwe siumakonda. Anditenga ine popanda kukuthokoza iwe.'

Ali chomwecho amayang'ana mozungulira iye ndi ludzu lokhala ngati mtima wake ukupsa.

Ali mmazunzo chonchi Satana wotembereredwa amapezerapo mwaŵi umene amasangalala kuwugwiritsa ntchito: Ndi chikho cha madzi m'manja mwake amabwera pafupi ndi bedi la munthuyo ndi cholinga chomubera iman yake.

Amagwedeza chikho cha madzi ozizira oundana m'menemo pafupi ndi bedi la wodwala. Wodwalayo amamuwona ndipo amamva madzi akugwedezeka. Iyi ndi nthawi yomwe pamaoneka kisiyana kwa munthu wosauka ndi wolemera.

Ngati munthuyo alibe sa'adat, amati: 'Ndiloleni ndimwe madzi amenewo.' Ndichani angafunenso otembereredwayo! Mdyerekazi amanena: 'Nena kuti –hasha– Dziko lonse lilibe mlengi! Ngati wofookayo ndi munthu wa shaqi, amanena zomwe wawuzidwazo, ndiye kuti iman yake yatayika. Koma poti hikmat (Nzeru) zirli mu Huda (ya Allahu ta'âlâ), anthu oyang'anira matenda otere ayenera kusunga madzi pafupi. Pafupipafupi pakamwa pa wodwalayo payenera kutsegulidwa ndipo ayenera kupatsidwa madzi.

Ngati hidayah ikamupulumutsa, amatemberera Satana ndikukana madzi akewo.

Ngati nthawi yake yakwana - ndipo kuti iye ndi wokhulupirira - Azrail "alaihim-salâm" amalamulidwa kuti atulutse mzimu wake ndipo mngelo wodalitsikawo amakwaniritsa lamuloli. Angero mazana atatu ndi mphambu makumi asanu ndi limodzi (360) amalandira mzimu (wa wamwayiwo) kuchokera m'dzanja la Azrail "alaihim-salâm" ndipo onse amaoneka ngati abwenzi ndi anzake okondedwa a womwalirayo. Amauveka mzimu wakewo zobvala za ku mParadiso ndikuutengera ku

Nyumba ya chifumu ya ku Paradiso ndikuusonyeza malo ake ku mParadisoko. Ndipo mwachangu amautenga ndikukaubwezeretsa mu mtembo uja.

Ngati amwalira opanda iman, angelo mazana atatu ndi makumi asanu ndi limodzi (360) ochokera ku sijjin[1] amabweretsa masamba a (mtengo wa ku Jahannama wotchedwa Zaqqum[2] omwe ndi wakuda kwambiri kuposa phula. Amakulunga mzimu wake mmenemo ndipo mosazengereza amapita nawo ku Jahannama kukausonyeza malo ake, ndi kubwerera nawo kukausiya mu mtembo.)

Munthu akafika pa msinkhu wakutha msinkhu, nakhala ndi moyo wautali padziko lapansi, kusamamvera malamulo, ndi kusiya moyo wa pa dziko popanda kupanga tawba –auzu billah (Allah atiteteze ku mathero amenewa) akuona zilango zonsezi. Amakumana ndi zonyansa zonse, ndi kukathera ku Jahannama, pokhapokha ngati hidayah (chitsogozo) chochokera kwa Allahu ta'âlâ chitamupulumutsa kapena wadalitsidwa ndi shafa'at Muhammadi "sallallâhu alaihi wa sallam". (Chonde onani mutu wa makumi atatu ndi mphambu zisanu wa gawo la chiwiri m'bukhu la Endless Bliss kuti mudziwe zambiri za shafa'at[3] [kupembedzera].)

MFA YA ANA (OSACHIMWA)

Mwana wa Chisilamu akadwala ndikumwalira, malo ake ndi Maqam-i-illiyyin, komwe kuli ku mParadiso. Angelo 360 amabwera kuchokera kumeneko, naima pamizere patsogolo pa mwanayo, nati kwa iye: "Ya Masum (Ee, iwe mwana wosalakwa)! Uthenga wabwino kwa iwe! Lero ndi tsiku limene uyenera kudandaulira Haqq ta'âlâ za mbiriyako, za makolo ako, azigogo ako ndi anansi ako. Pamenepo angelo zana amamuveka chisoti cha shafa'at pa mutu pake, ndipo angelo zana limodzi amamuveka chisoti cha chikondi ndipo angelo ena amamuveka chobvala cha changu ndi champhamvu, ndipo angelo ena makumi asanu ndi limodzi amachinga katani ku maso ake.

Zotchinga zonse zikangotukulidwa, amaona makolo ndi azigogo onse a okhulupirira onse akale kuyambira Hadrat Adam, komanso

[1] Kumalo komwe mizimu ya anthu osakhulupirira izasungidwe mpaka tsiku la kuuka kwa akufa

[2] Mmtengo omwe umachokera pansi pa moto ku Jahannama.

3 Ntchito yochonderera kwa Allah kudsera mwa bwenzi lapamtima la Allah kuti akhulukidwe wochimwa wokhulupurira

mazunzo okonzekera ena a iwo. Akawona zoona izi ndi zomwe zikuwakhuza anthuwo, amalira ndi kunjenjemera, kotero kuti anthu osadziwa tanthauzo la zochitikazi amaona ngati akutatha ndi imfa.

Akabwera angelo ochotsa mzimu wake ndikuuona atavekedwa chisoti cha shafa'at, ndi nsalu yotchinga moyang'anizana ndi maso ake, iwo amalephera kutululutsa mzimu wake ndipo amanena kwa iye: "Ya Ma'sum! Khallaq-i-'alam (Mlengi wa zolengedwa zonse) akupereka salam kwa iwe ndi kukufunirani zabwino), akunena kuti: "Ndinachilenga, ndipo chiloleni chibwerere kwa Ine." Pakuti ndinachipatsa mzimu wake kuti usungidwe bwino, ndipo tsopano ubwezeredwe kwa Ine. Ndipo ndiloleni ndiupatse Mparadiso ndi didar (Kundiona Ine) gati mphoto yake. Ngati simukutikhulupirira ife tembenuzirani nkhope yanu kumwamba, kuti mudzionere."

Pamenepo mwanayo amayang'ana ndikuona angelo ndi Kukongola (Jamal) kwa Allahu ta'âlâ. Amanjenjemera, kuchita thovu m'kamwa, ndipo thupi limasintha ndi chisangalalo. Chisangalalo chake chachikulu kwambiri choti kutsala pang'ono kulumpha ndi kuthamangira kukapereka mzimu wake, pomwepo amaona makolo ake ali m'masautso, ndipo amakana kupereka mzimu wake. "Ya ma'sum," akutero angelowo! "Bwanji usakupereka mzimu wako?" Mwanayo akuti: "Inu angelo! Ndipemphereni kwa Allahu ta'âlâ m'malo mwanga kuti awakhululukire abale anga ndi makolo anga." Angero akunena: "E, Rabbi! Mukudziwa zimene tili nazo ndi mwana wosalakwayu." Pamenepo Hadrat Allah 'jalla shanuhu' amawayankhula kuti: **"Ndithu, chifukwa cha 'Iz yanga** (mphamvu, ulemerero), **ndawakhululukira."** Kenako angelowo amatembenukira kwa mwanayo n'kunena kuti: "Ya ma'sum! Uthenga wabwino kwa iwe! Allahu ta'âlâ wakhululukira amene adali ndi Iman ndipo wavomereza zopempha zako zonse." Pamene mwanayo amasangalala ndi nkhani yabwinoyi. Haqq ta'âlâ amatumiza kwa iye ma **huri** awiri kuchokera ku Paradiso. Akuoneka ngati makolo ake ndipo amaonekera kwa mwanayo, akutatambasula manja awo, nati: "E, iwe mwana wathu! Bwera ndi ife! Sitingathe kukhala popanda iwe ku m'Paradaiso." Iwo amampasa mwanayo apozi yemwe amabweretsa kuchokera ku Paradaiso ndi kumuuza kuti, "Taona, tenga." Pamene mwanayo akumva fungo la apoziyo, Hadrat Azrail "alaihim-salâm" (Mngelo wa imfa) amasunduka mwana wosalakwa ndi mwachikondi ndipo amachotsa mzimu wamwanayo nthawi yomweyo.

Malinga ndi mafotokozedwe ena, mwanayo akamva fungo la apozi, mzimu wake umakakamira pa apozipo ndipo Mngelo wa imfa

amatenga mzimu wa mwanayo pa apoziyo. Malongosolredwe onse ziwiri ndi ololedwa.

Zikatero Mngelo wa imfa amatenga mzimuwo kupita nawo ku Paradaiso. Mzimuwo umanka niuwona kumwamba m'njiramo. Kumeneko kuli dziko lalikulu lotambasuka lopangidwa ndi miyala yobiriwira ya chrysolite. Akafika kumeneko mwanayo amafunsa: "Ndi chifukwa chiyani mwandibweretsera kuno?" Angelo afotokoza kuti: "Ya ma'sum! Uko kuli malo okwera. Ndikotentha kwambiri kumeneko. Dziko lalikululi liri ndi akasupe achifundo zikwi makumi asanu ndi awiri (70,000). Ima pafupi ndi dziwe lodala la Hadrat Rasul akram "alaihim-salâm" ndipo muwone matambula a galasi owala! Makolo ako akadzafika pamalo okwerawo, uzidzatira madzi m'matambula a galasi awa ndi kuwapatsa. Uzizawagwiri apa, osawalola kupita, kuopera kuti angapite ku Jahannama ndi kuzunzidwa ndi chilango. Poti mapemphero amene mukupemphera ndi ovomerezeka kwa Haqq ta'âlâ. Ndipo usiku wa lachisanu (usiku wa pakati pa lachinayi ndi lachisanu) utsike kupita pa dziko lapansi. Ukapita kumeneko kapereke salaam za Allahu ta'âlâ ku Ummat Muhammad "sallallâhu alaihi wa sallam". Ndipo kawazeni nuru kwa iwo ndipo katenge chiyamiko chawo kwa Allah ta'âlâ."

Akamaliza kuonetsa mzimu wa mwanayo zonsezi mofulumira amabwerera nawo ndi kuyika pa mbali pa mutu wa mwana wakufayo.

Muzochitika zonse monga kuswalira janaza, kuyika mtembo, ndi kufunsa mafunso m'manda, mzimu umakhala pamwamba pa manda. Ngati makolo ake amwalira opanda iman, padzakhala nsalu yotchinga pakati pa makolowo ndi mwanayo. Mwanayo samawafunafuna kapena kukumana nawo kulikonse, kotero kuti amalakalaka atawonana. Izi ndi zoona zake za ana a Asilamu omwe amamwalira asanakwanitse zaka zakutha msinkhu.

IMFA YA MZIMAYI WA CHISILAMU

Mkazi amene amakhala moyo wosadzionetsera kwa amuna omwe anali na-mahram kwa iye, asanaziphimbe moyenera, koma kuti amaphimba thupi lake monga mogwirizana ndi chiphunzitso cha Chisilamu ndipo yemwe mamuna wake akusangalala naye, amamwalira imfa ya ulemu. Mkazi wotere akamwalira atangobereka, kaya ali ndi mimba, kaya chifukwa cha muliri, kaya chifukwa cha kuvutika kwa mkati kapena wamwalira ndi imfa yachibadwa, pa nthawi ya imfa yake kumadza angelo a ku mParadiso ndi kuima

m’mizere patsogolo pa iye. Amamupatsa Salaam mwaulemu ndi kumuuza kuti; “E, iwe, mzimayi wokondedwa ndi wofera chikhulupiriro cha Allah Subhana Watala! Tulukani, mukuchita chiyani m'nyumba ya chifumu ya pa dziko lapansi? Allah Subhana Watala wasangalala nanu ndipo wakukhululukirani machimo anu chifukwa cha matenda anu ndipo wakupatsani Paradiso Yake. Bwerani ndipo dziperekeni kuti musungike bwino!” Mkaziyo akawona ulemerero womwe akukakhala amafuna kupereka mzimu wake. Koma amadzayang’ana mozungulira iye nanena: “Allah Subhana Watala aweruze kaye anzanga m’dziko la pansi ndi chisoni, kenako ine ndidzapereka mzimu wanga.”

Angelo amapereka pempho la mzimayilo kwa Janab-i-Haqq. Ndipo mau a Allah Subhana Watala amazionetsera okha kuti: "**Chifukwa cha Ukulu Wanga, Ndavomereza mapemphero onse a kapolo Wanga uyu."** Ndipo Angelo amapereka uthenga wabwinowu kwa mzimayiyo. Nthawi yomweyo Mngelo wa imfa ndi angelo zana limodzi ndi makumi awiri (120) achifundo amafika. Nur (kuwala kwa) nkhope zawo kumafika ku Arsh (mpando wa chifumu). Amavala nduwira za ufumu pa mitu yawo, zovala za Nur (zowala), nsapato za golide, ndipo amakhala ndi mapiko obiriwira. Amatenga zipatso za ku Paradiso m’manja mwawo zomwe zimanunkhira bwino ngati musk wopakidwa pa iwo. Amatsika ndi kupereka salaam mwaulemu ndi mwachifundo, nati: “Khallaq-i-’alam (Mlengi wa zolengedwa zonse) akupereka salaam kwa inu, akukupatsani mParadiso, kukupangani kukhala woyandikirana ndi wokondedwa wake Mtumiki Muhammad “sallallâhu alaihi wa sallam” ndi kukhala bwenzi la Hadrat 'Aisha.”

Pa nthawi yomwe mzimayi wa iman uyu akumva zomwe zikunenedwa kwa iye, makatani pa maso ake amatseguka ndipo amaona azimayi a Iman mbali imodzi ndi ena omwe akuzunzidwa chifukwa cha machimo awo mbali ina. Choncho iye amapempha: “Chonde akhululukireni machimo awo, Ee Mbuye wanga!” Pamenepo mau ochokwera kwa Janab-i-’izzat (Mbuye wolemekezekayo) amamveka: “E, iwe Jariyah (kapolo wachizimayi) wanga! Ndakwaniritsa zokhumba zako zonse. Tsopano pereka mzimu wako kuti ukasungidwe ndi mkazi wa Wokondedwa Wanga (mkazi wa Muhammad “sallallâhu alaihi wa sallam”) ndi mwana wake mwana wamkazi (Hadrat Aisha) ali okonzeka ndi kukulandira.” Mzimayiyo akamva mau awa amayesera kupereka moyo wake, mzimu wake umanjenjemera, mapazi ake akuthamangira kutsogolo, ndipo iye amatuluka thukuta. Iye akuti apereke moyo wake, Angelo aŵiri

amawonekera pamenepo. Aliyense wa iwo atatenga ndodo ya moto m'manja mwake. Amaima wina kudzanja la kumanja ndipo wina kudzanja la kumanzere. Nthawi yomweyo, Satana wotembereredwayo amafika pamalopo akuthamanga, akulankhula yekha nati: "Sindikuyembekezera zambiri kwa ameneyu, koma ndione!" Amabwetsa mphika wopangidwa ndi zokongoletsa ndikuonetsa. Umakhala wodzadza ndi madzi oyera ozizira bwino. Angelo aja akaona cholengedwa choipacho amaphwanya mphikawo ndi ndodo zao zija ndi kumuopseza. Mkazi wa chisilamuyo amaseka akaona izi. Kenako ma **huri** (anamwali okongola a ku mParadiso) amamupatsa chakumwa chake chochokera ku dziwe la Kawthar (dziwe la ku Mparadiso). Kapu yake imakhala yopangidwa ndi zokongoletsera za mtengo wapatali. Mzimayiyo amamwa chakumwa cha ku mParadisocho chomwe ndi chokoma kwambiri kotero kuti mzimu wake umalumpha ndikukakamira pa kamwa pa kapuyo. Pamenepo Mngelo wa imfa amautenga kuchokera pa kapupo. Angelo amalengeza za imfa ya mzimayiyo wina kwa mnzake, nati: **"Inna lillahi wa inna ilaihi raji'un!** (Ndithu ife tinachokera kwa Iye, ndipo kwa Iye tidzabwerera). Ndipo mzimu wa mzimayiyo umatengedwa pa ulendo wopita kumwamba ngati mlendo wokaona malo. Kumeneko amakaonetsedwa malo ake okhala ku m'Paradaiso, nabweranso ndi mzimu mosakhalitsa ndi kuuika pa mutu pa mtembowo.

Pamene osambitsa akumuvula zovala zake ndi kumasula tsitsi lake, mzimu wake umabwera ku mutu kwa mtembo wake ndikunena kuti: "E, iwe munthu wosambitsa! Mgwireni mosamala! Pakuti walandira chilonda cha imfa kuchokera kumaphazi a Azrail (Mngelo wa imfa). Ndipo khungu langa liribe mphamvu ndipo ndi lotopa chifukwa ja momwe landadutsa." Thupi likatengedwa kupita ku chitebulo chosambitsira mzimu umabweranso ndikuzati: "Madzi asakhale otentha kwambiri! Khungu langa ndi lofooka ndithu. Manja anu asandipweteke ndipo ndithandizeni mwamsanga, kuti ndipeze mpumulo!" Mtembowo ukasambitsidwa ndi kuvekedwa, mzimu umadikira kwa kanthawi pang'ono ndi kunena kuti: "Aka ndi komaliza kuona dziko. Ndiloleni ndione anzanga ndi abale anga ndipo aloleni andione kuti imfa yanga ikhale chenjezo kwa iwo. Popeza iwonso adzafa posachedwa, monga ine. Asalire kapena kubuula pa mbuyo panga. Asandiiwale, ndipo andikumbukire nthawi zonse. Awerenge (kapena kukumbukira) Qur'an al-kareem (ndipo atumize thawab zantchito zawo za bwino kwa ine). Asalimbirane chuma chomwe ndasiya kuti ine ndisazunzike m'manda chifukwa cha mikangano yawo. Andikumbukire lachisanu ndi masiku a 'Eid."

Chitanda cha maliro chikayikidwa pa **musalla** (malo ochitira Swalah ya Janaza]), mzimu umayankhula: “Masukani, Ee inu ana anga amuna ndi akazi ndi makolo anga! Palibe tsiku lina la kulekana lomwe lingafanane ndi ili. Tidzasowana koma tidzakumananso posachedwa pa tsiku la kuuka. Tsalani bwino, inu anthu amene mukundilira ine!”

Pamene chitanda cha maliro chikukwezedwa m’mapewa, mzimu wake umaitananso kuti: “Ndinyamule modekha! Ngati cholinga chanu chili chopeza thawab, musandigunyuzegunyuze! Ndinyamuleni mondisangalatsa kuti nditenge kundisangalatsa kwanuko kwa Allah Subhana Watala!”

Chitanda cha maliro chikafika kumanda ndi kuikidwa pafupi ndi manda, mzimu wa mzimayiyo umaitananso kuti: “Taonani mmene ndiliri ine; ili likhale chenjezo kwa inu! Tsopano mundiika mu mdima ndi kunsiya ndekha. Ndidzakhala ndekha ndi **amali** zanga (ntchito zanga). Onani nthawi yowawitsa ngati ino, muopeni Allah Subhana Watala ndipo musatengeke ndi kunyengeka ndi za dziko loipali!”

Mtembo ukayikidwa m’manda, mzimu umakhala pamalo pake, pa mbali pa mutu. Munthu wakufa asayikidwe m’manda mwawo popanda kosoma talqin. Ndi ntchito ya sunnah kwa Msilamu wa salih kuchita ntchito yotchedwa Talqin makukakwilira.

Ma Wahhabi amakana zoti ndi kubwereza talqin ndi Sunnah. Akuti kutero ndi bid’ah (kuonjezera nzeru za tsopano pa nkhani za chipembezo). Amati munthu wakufa sangamve. Koma akatswiri a Ahl Sunnah “rahima-hullâhu ta’âlâ” analemba mabuku osiyanasiyana otsimikizira kuti ndi sunnah kuwerenga talqin. **Nur-ul-yaqin fi mebhas-it-telqin** ndi limodzi mwa mabuku ofunikawa. Linalembedwa ndi Mustafa bin Ibrahim Siyami“rahima-hullâhu ta’âlâ” ndipo linasindikizidwa ku Bangkok, Thailand mu 1345. Kope lake lachiwiri linatulutsidwa ku Istanbul, Turkey, mu 1396 (1976 A.D.). Hadith sharif mwaulamuliro wa Tabarani ndi Ibni Menda yatchulidwa bukhu limeneli. Hadith-i-sharif imeneyo ikulamula kuchita talqin. Ndi ulamulo wa Allah Subhana Watala, mtembo umadzuka m'manda ngati unali m'tulo, ndi kukhala mu mdimamo. Umayitana wa ntchito wake kapena kapolo wake kapena munthu amene ankamutumikira m’dzikoli ndi kunena kuti: “Ndibweretsera kandulo!” Ndipo sadzayankhidwa. Manda amang’ambika pakati ndipo Angelo awiri amaonekera, Angelo ofunsa mafunso, **Munkar** ndi **Nakir.** Mkamwa mwawo mumatulika malaŵi a moto ndipo m’mphuno mwawo mukutulutsa utsi. Iwo amafika pafupi ndi wakufayo ndikumufunsa kuti: **“Man Rabbuka? wa ma dinuka? wa man nabiyyuka,**” (Mbuye wakondi ndani,

chipembedzo chanu ndi chiti, ndipo Mneneri wanu ndani)?" Ngati ayankha bwino mafunsowo, Angelo amamuuza nkhani yabwino ya chifundo cha Haqq ta'âlâ, ndikumapita. Nthawi yomweyo ku dzanja la ku manja kwa manda kumatseguka zenera ndipo wina amene nkhope yake yowala ngati mwezi wathunthu amalowa pa zenerapo.

Mzimayi wodalitsika ndi iman uyu akangoona munthu wokongola ameneyu pambali pake, amasangalala ndi mlendo wosayembekezerayo ndipo amafunsa kuti: "Ndi inu ndani?" Ndipo mlendoyo amayankha: "Ndalengedwa kuchokera mu kuleza mtima kwanu ndi chiyamiko chanu pa dziko la pansi. Ine ndidzakhala bwenzi lanu mpaka tsiku la kuuka kwa akufa."

Ngati moyo wathu ukupitirizabe kuyanjana ndi za Haram!,
Mtima wathu siudzaona kuwala kochokera kwa Allah!

IFA YA OFERA CHIKHULUPILIRO (WOLAKWILIDWA, WODEKHA, NDI GHARIB [OSUNGULUMWA])

Imfa za anthu onsewa ndi zofanana. Kulongosola imfa ya mtundu umodzi kudzayimira zonse poti ndi zofanana momwe zimachitikira. Kotero telongosola za imfa ya gharib.

Pali mitundu iwiri ya anthu a gharib (wosungulumwa). Mtundu woyamba ndi munthu wokhulupirira yemwe wasiyidwa yekha ku dziko lakutali ndipo alibe wachibale kapena wodziwana nawo. Mtundu wachiwiri ndi munthu wokhulupirira wosauka, ngakhale akukhala kwawo koma anthu samakamuzonda. Okhulupirira onsewa ndi anthu a gharib. Ngati atamwalira ali choncho adzakhala munthu woti wafera chikhulupiriro. Munthu yemwe wakwanisa zaka makumi asanu ndi limodzi (60) ndipo samaphonya Swalah zisanu pa tsiku amafa ngati ofera chikhulupiriro. Munthu amene wamwalira akuchita za haram sadzakhala wofera chikhulupiriro. Mwachitsanzo, munthu amene wafa tamwa mowa mpaka kufa nawo; Munthu wotere sitinganene kuti wofera chikhulupiriro. Koma ngati munthu wamwalira pa nthaŵi ya kumwa moŵa chifukwa choti nyumba imene amamwera mowa yagwa, ameneyo wafera chikhulupiriro. Mtundu wina wofera chikhulupiriro ndi mtsikana kapena mzimayi amene samatuluka mnyumba asanaziphimbe bwino mutu, tsitsi, mikono ndi miyendo. Kumbukirani kuti thupi la mkazi lonse, kupatula nkhope ndi zikhato zake ndi ziwalo za awrat (ziwalo zobisika). Ndi fardh kwa mzimayi

kubisa thupi lake lonse, kupatula nkhope yake ndi zikhato zake pamene akutuluka mnyumba kapena ali pa maso pa amuna amene ali na-mahram kwa iye. Mkazi amene salabadira izi amakhala wosakhulupirira. Malamulo ndi zoletsedwa za Allahu ta'âlâ, pamodzi zimatchedwa **Ahkam islamiyya**. Makolo amene amaphunzira Ahkam islamiyya kwa ana awo ali m'gulu la anthu ofera chikhulipiriro. Msilamu amene wamwalira ali m'ndende atagwidwa ndi adani naye amakhala kuti wofera chikhulupiriro. Wosakhulupirira amene wamwalira mozunzika, sangakhale wofera chikhulupiriro. Munthu akafa ali wosakhulupirira sadzalowa ku mParadiso.

Wofera chikhulupiriro wina ndi Msilamu amene amatembenukira nkhope yake ku Darghah-i-'izzat napempha kuti: "E, iwe Ma'bud wanga, yemwe ndikulambira)! Mmoyo wanga wonse sindinakhale ndi chiyembekezo mwa wina aliyense koma mu ukuu wanu. Sindinayike mutu wanga pansi (Sajida) kulambira wina aliyense woposa inu. Ndipo sindinagonjerepo kwa onyenga aliyense ngakhale Satana yemwe ali mdani. Ooh mbuye wanga! Ndikuyembekezera kuti mudzapatsa Ummat-i-Muhammadi "sallallâhu alaihi wa sallam" 'afw (chikhululuko) ndi maghfirat (chifundo)". Munthu uyunso ndi wofera chikhulupiriro. Onsewa sadzakhala ofera chikhulupiriro pokhapokha atakhala ndi iman monga zaphunzitsidwira ndi akatswiri a Ahl sunnah (anthu a sunnah) komanso kuti akuchita Swalah kasanu pa tsiku.

Nthawi yomwe anthu tawalongosola apawa akuyika mitu yawo pa pilo pa bed yomwe afere, zipata za kumwamba zimatseguka ndipo Angelo ambiri amatsika padziko lapansi. Allah Subhana Watala yekha ndi amene amadziwa chiwerengero cha Angelowo. Amanyamula zisoti za chifumu ndi zovala za nur (zowala) m'manja mwawo. Mwaulemu waukulu amayitana mzimu wa munthuyo. Haqq ta'âlâ akufotokoza za izi kumapeto kwa Sura Fajr.

Angelo odalitsika amakulunga mzimu wa munthu wamwayiwo mu zovala zomwe abwera nazo. Liu lochokera kwa Haqq ta'âlâ limamveka kuti: "Tengerani mzimu umenewo ku mParadiso, poti iye amakonda kupanga Swalah kuposa ena, amakonda kulandira alendo, ndipo amakhululukira anthu akamulakwira komanso amkachita Istighfar pafupipafupi. Iye amachita dhikr (kuzipereka/kuyamika) kwa ine kwambiri. Samatuluka mnyumba osavala mosalongosoka ndipo amapewa haram. Ndipo amamvera Atumiki ndi Chisilamu padziko lapansi."

Angelo awiri, amabwera wina ku pewa la kumanja wina lakumamzere kwa munthuyo. Awa ndi Angelo osunga kaundula wa

zabwino ndi zoipa za munthu. Iwo amapempha: “O Ambuye! Munatipatsa udindo woyang’anira munthu uyu dziko lapansi. Tsopano tilolen tikwere kumwamba ndi mzimu wa munthuyu.” Liwu lochokera kwa Wam’mwambamwamba limanena: “Inu khalani pa manda a munthu ameneyu. Chitani ma tasbih ndi takbir. Pangani sajda ndikumupatsa thawab (za ntchito zake zopembeza) kapolo Wanga.” Pamenepo iwo amapanga dhikr ndi tasbih mosalekeza ndipo amalemba thawab m’buku la munthu ameneyo. Izi zimapitirira mpaka kumapeto kwa dziko.

MFUNDO YOFUNIKA: Ma munafiq (wosakhulupirira) okhala mu Egypt anagalukira utsogoleri wolungama wa Khalifa Uthman “radiyallâhu ’anh” ndipo anabwera ku Madina kudzamupha. Anthu othandiza ma munafiq ananena mabodza ndi miseche. Ananyoza Sahaba pofalitsa miseche kuti ‘Asilamu aku Madina sanathandize Khalifa.’ Zoona zake ndi zoti Khalifa amafuna kupeza ulemelero wopambana ku mParadiso, kuti akakhale wapamwamba mwa anthu onse ofera chikhulupiriro. Ili linali pemphero lake kwa Allah Subhana Watala, kuti adalitsidwe kwambiri. Asilamu ena anabwera kuti amuthandize koma iye anawapempha kuti asamuthandize. Khalifa anaphedwa mosavuta ndipo potero anakwanilitsa zofuna zake. Allahu Subhana Watala analandira pemphero lake.

Ofera chikhulupiriro samamva ululu uliwonse akamamwalira. Iwo amaonetsedwa madalitso amene adzapatsidwe ku m’Paradaiso, kotero kuti amapereka mzimu wawo mofulumira kwa Angelo pamene akukondwera ndi malipiro omwe akuwayembekezera.

IMFA YA MUNTHU WOSAKHULUPIRIRA

Anthu awa akatsala pang’ono kumwalira, munthu wosakhulupirira; munthu amene watuluka Chisilamu; munthu yemwe amati Qur’an al-kareem ndi malamulo a m’chipululu; munthu yemwe ali mbuli ndi wosalongosoka womanyoza Muhammadi “sallallâhu alaihi wa sallam” yemwe ndi wolemekezeka komanso bwana wa Atumiki onse kuti ndi mbusa wa ngamira (–Allah Subhana Watala atiteteze ku mchitidwe wamanyazi wotere); munthu amene amaimirira ndi kunena kuti zipembedzo ndi zosafunikira chifukwa cha kuunika kwa Chisilamu,maziko a mtendere ndi chisangalalo cha anthu, gwero la chidziwitso, makhalide , ukhondo, thanzi ndi chilungamo, ndi wolimbikitsa zikhalidwe zonse - zopangidwa pansi pa njira zosautsa za ubongo womwe uli wonyansa ngati bokosi la mitembo ndi munthu yemwe amalamulidwa ndi nafs zake, akatsala pang’ono kufa, katani

lotchinga pamaso pake lidzakwezedwa. Amaonetsedwa ku mParadiso. Mngelo wokongola amanena kwa iye: “E, iwe wosakhulupirira! E, iwe, munthu wonyozeka, umawanena Asilamu kuti ‘anthu opusa’. Unali ndi anthu omwe amatsata zilakolako zawo ndi kupondereza mfundo zabwino. Ndithu munali m’njira yolakwika. Wakhala ukunyoza Chisilamu chomwe ndi chipembedzo cholondola. Awa ndi malo a anthu okhulupirira, omwe amalemekeza ziphunzitso zomwe Muhammadi “sallallâhu alaihi wa sallam” anabweretsa kuchokera kwa Allah Subhana Watala. Iye amaona madalitso a ku m’Paradaiso. Ndi anamwali (huri) aku Paradiso amati: “Anthu amene ali ndi Iman adzapulumutsidwa ku chilango chimene Allah Subhana Watala adzapereke.” Kenako Satana amaonekera kwa iye ngati wansembe ndi kunena kuti: “Iwe mwana wa awuje! Awa anali apawa ndi a bodza. Madalitso amakuonetsawa adzakhala ako.” Kenako Jahannama idzaonekera kwa iye. Kuli mapiri amoto, zinkhanira ndi anamkalizi akukuakulu. Amaona mazunzo amene anenedwa mu Hadith sharif. Angelo ozunzo aku Jahannama otchedwa Zabaniyah akuthyapula ochimwa ndi ndodo zamoto. Mkamwa mwawo mukutuluka malaŵi a moto. Iwo ndi atali ngati minareti. Mano awo ngati nyanga za ng’ombe zamphongo. Kuitana kwawo kumveka ngati bingu. Wosakhulupirirayo amanjenjemera ndi mawu awowo ndi kutembenukira kwa Satana kuti mwina angawapulumutse. Satana naye ali ndi mantha moti akutembenuka ndi kumuonesa mchira. Angelo amagwira Satana ndi kumugwetsa pansi. Kwa wosakhulupirira amanena: “E, iwe mdani wa Chisilamu! Pa dziko wakhala ukukana Mtumiki wa Allah Subhana Watala. Tsopano iwe ukukana Angelo ndipo Satana wotembereredwa akukunyenga iwe.” Amamveka unyolo wa moto mkhosi mwake. Amamukoka miyendo yake chakumbuyo kotero kuti mapazi ake amakhala kumbuyo kwa mutu wake tsopano. Dzanja lake lamanja amalilowetsa ku manzere kwa chifuwa chake ndipo dzanja lake la manzere amaliyika pa mimba pake mbali ya kumanja ndi kutululutsa manja ake onse kuchokera kumbuyo kwake.

Pali ayati karima yomwe ikufotokoza zochitika zochititsa mantha izi. Wosakhulupilirayo amalira uku akuyitana osyasyalika ake kuti amuthandize. Angelo ozunza amamuyankha: “E, iwe wosakhulupirira, iwe ndi chitsiru. Umanyogodola Asilamu! Ino si nthawi yopempha. Iman kapena mapemphero sizidzalandiridwanso. Ino ndi nthawi yoti ulangidwe chifukwa cha kusakhulupirira kwako.” Amamukoka lilime lake kuchokera kumbuyo kwa khosi. Amamuchotsa maso ake. Amamuzunza mnjira zambiri zowawa kwambiri. Ndipo amachotsa mzimu wake mwankhanza ndi kuuponya ku Jahannama. Allah

Subhana watala atidalitse kuti tithe kupereka mizimu yathu ku chipembedzo cha Muhammad “sallallâhu alaihi wa sallam” ndi kukhala okonzeka ndi chikhulupiliro cholembedwa m’mabuku akatswiri a Ahl sunnat amene adafikitsa chipembedzo cha olemekezekayo kwa ife molondola. Amin.

Aliyense adzafa ngakhale atakhala moyo wawutali bwanji. Mtumiki “sallallâhu alaihi wa sallam” ananena kuti: **“Pamene mzimu wa munthu ukutuluka m’thupi lake, liwu limati: E, iwe munthu! Kodi walisiya dziko kapena dziko lakusiya iwe? Walisonkhanitsa dziko lapansi, kapena dziko lapansi lakusonkhanitsa iwe? Wapha dziko la pansi kapena dzikolapansi lakuphani? Mtembo ukayamba kusambitsidwa, mau amafunsa mafunso atatu:**

1– Lili kuti thupi lako lamphamvu lija? Chakufooketsa ndi chani?

2- Malankhulidwe ako okoma aja ali kuti? Ndi chiyani chakukhazika chete iwe?

3- Anzako okondeka aja ali kuti? Chifukwa chiyani akusiya iwe wekha?

Pomwe mtembo ukuvekedwa, liu lina limanena: Usanyamuke ulibe zokuyenereza. Ulendo uwu ndi wosabwerera. Siudzabwereranso mpaka muyaya. Ukupita komwe kwadzadza ndi Angelo omwe amapereka zilango. Mtembo ukaikidwa mu Chitanda liwu lina limanena: Nkhani yabwino kwa inu ngati mwakwaniritsa kukondweretsa Janab Haqq. Ulemelero ndi chisangalalo zikukuyembekezerani! Koma tsoka kwa iwe ngati uli ndi mkwiyo wa Janab Haqq! Pomwe chitanda chafika pafupi ndi manda, liwu lina limti: E iwe munthu! Wakhonza chanji pa moyo wa dziko lapanso choti chikuthandize mmanda? Kuwala kwanji wabweretsa kuti uwunikire mmalo a mdimawa? Ndi chani wabweretsa kuchokera mu chuma ndi kutchuka kwako? Watenga chani choti uzikhalira ndi kuyala mmalo olimba ngati awa? Mtembo ukaikidwa m’manda, manda amayamba kulankhula nati: Umkayankhula pa nsana panga koma lero uli chete m’mimba mwanga. Ndipo mwambo woyika mtembo m’manda ukatha ndipo anthu onse abwerera ku mudzi, mawu ochokera kwa Allah Subhana Watala akuti:

“E Kapolo Wanga, watsala wekha tsopano; akusiya wekha m’manda, mu mdima ndipo iwo apita. Anali abwenzi ako, abale ako, ana ako, ndi anthu omwe amakukonda iwe. Koma palibe yemwe ali waphindu kwa iwe tsopano. E iwe kapolo Wanga! Unali wosamvera Ine. Unali wokanira malamulo anga ndipo siumkaganizira zoti udzafika apa. Wakufayo ngati amwalira ali ndi iman, pali

chikhulupiriro choti Janab Haqq adzamdalitsa ndi kumukhululukira ndipo adzamuuza kuti: E iwe kapolo Wanga wokhulupirira! Sikoyenera mu Ukulu Wanga kukusiya uli wosungulumwa m'manda mwako. Mwa ufulu wa Izzat-u-jalal Wanga, Ndikuchitira chifundo chomwe chidzadabwitse abwenzi ako ndipo ndidzakuchitira chifundo choposa chifundo cha makolo pa mwana wawo. Ndi kukoma mtima Kwake kwapadera ndi chisomo Chake, amakhuluka machimo a kapolo wake onse, kotero kuti manda ake amakhala Munda wa mParadiso wodzala ndi huri ndi madalitso a mParadiso. Allahu ta'âlâ ndiwachifundo kwambiri moti amakhululukira a kapolo Ake ochimwa. Iye ndi wa chifundo kwambiri, amawona machimo a akapolo Ake akuchuluka kangapo koma amawaphimba m'malo mowatulusya kuti awonekere. Ndiye tiyenera titsatire malamulowo ndi kupewa zoletsedwa za Mlengi woteroyo ndi kudzipulumutsa tokha ku chilango chomwe chayandikira pochita amal-i-salih (ntchito zovomerezeka)".

Okhulupirira onse, Ochimwa ndi osachimwa, adzafunsidwa mafunso m'manda. Chilango chidzaperekedwa kwa amene sanalandire chikhululuko ndi osakhulupirira. Anthu amiseche pakati pa Asilamu ndi anthu omwe amadonthetsera mkodzo pa zovala zawo akamakodza adzazunzidwa m'manda. [Mazunzo a m'manda adzaperekedwa ku mzimu ndi thupi lomwe, (Mfundo zimenezi ndi zovuta kuzimvetsa ndi mphamvu za maganizo athu. Choncho tipewa kuyesa kuzimvetsa pogwiritsa ntchito maganizo athu.]

Ngati munthu amwalira alibe iman, (wosakhulupirira) adzalandira chilango chowawa mmanda mpaka pa mahsher (tsiku lachiweruzo), [ndi kenako wa kumoto kwa muyaya.]

Iyi ndi ndakatulo ya Ottoman wa ku Turkish m'Chichewa, yolembedwa ndi Abd-ur-Rahman Sami Pasha, mkulu wopuma mu ulamiliro wa yemwe anamwalira mu 1295 [1878 AD], ali membala wake wa Senate:

O iwe, mlendo wamoyo! Usapereke mtima wako kwa wina aliyense koma Allah ta'âlâ!

Palibe adzatsale padziko lapansi. Palibe angachite kanthu koma Allah yekha. Allah ta'âlâ yekha adzkala kwamuyaya.

Aliyense ali ndi zosamala, masiku okoma ndi owawa. Dziko lapasilino si lopikisanirana.

Inenso ndinali mthawi yanga, Ngati mphete ya mwala wamtengo wapatali ya

Kenako mtima wanga unayamba kudwala. Mphamvu zanga zinatha. Pomaliza mbalame ya moyo wanga (mzimu wanga) inawuluka. Pakuti, khola (thupi langa) linali litaphwanyika ndi kuonongeka.

Thanzi langa ngati kandulo, linazima. Mdima unali kundizungulira. Dzuwa ladziko linali linatuluka. Zonse zinaunikiridwa ndi kuwala kwa Allah.

Tsopano ndinapeza mbuye wanga. Machimo anga anawonekera. Nditapempha chikhululuko, Anakumana nane mwa chifundo chake chosatha.

O Rabbi, Ndinachita machimo osaweregeka. Koma ndinazikhulupirira ndeka ndi nkhope yanga yakudayi, kuchipata chanu chapamwamba kwambiri. Chonde ndikhululukireni.

Lero [1286] pomwe ndikulema, ndapanga dzina lanu Ghafur. Tanthauzo lake lidzakhala loona. Ndi Alla yekha angathe kupanga chinthu. Palibe wina koma Allah yekha ndi wamuyaya.

Moyo uno ndi maloto odazla ndi zowawa
Sitinabadwe kuti tidzafe?
Patapita maola oceoa a chisangalalo,
Kuthamangitsa chisangalalo chirichonse chopezeka.

Mwa umbuli nthawi zonse timamira
Kuphompho la imfa mwachangu
Kumira mmavuto ndi mziphinjo,
Dziko limatikhankhira ku ukafiri

Ndipo if osauka powona nyumba iyi
Tifunse komwe okhalamo akuchokera
Mulengi wake, zolengedwa zake, zinsinsi zake,
Magwero obisika, zomwe ndi zodabwitsa.

Koma zinsinsi zobisika ndi Haqq mwiniwake
Ndi zopyola malingaliro a kapolo,
Munthu wa chidziwitsa chopanda pache, cholephera
Adzalakwitsidwa mwachinyengo.

KUKAZONDA KU MANDA NDI KUWERENGA QU´RAN AL-KAREEM

Kukazonda ku manda ndi Sunnah. Manda ayenera kuzondedwa kamodzi pa sabata kepena masiku a Eid. Tsiku lopatsa thawb zochuluka ndi la Chinayi, la chisanu ndi loweluka. Zalembedwa mmasamba omalizira a bukhu la **Shir'at-ul-Islam**, lolembedwa ndi Muhammad bin Ebi Bakr "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih", d. 573 [1178 A.D.], Bukhara,) kuti ndi sunnah kuzonda ku manda. Wokazonda ku manda akumbukire kuti mitembo imawola, ndipo izi zikhale chenjezo. Nthawi iliyonse Uthman "radiyallâhu 'anh" amadutsa pa manda, amalira kwambiri moti ndevu zake zimanyowa ndi misozi. Powonjezera chenjezo, wokazonda adziwenso kuti anthu akufa amapindula ndi madalitso onenedwa pa iwe. Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" amakazonda manda a abale ake ndi a ma sahaba ake "radiyallâhu 'anhum" . Pambuyo popereka salaam ndi kupereka mdalitso ndi kupanga dua, wozondayo amakala nkhope yake atayang'ana ku mandapo ndi nsana wake utalodza ku Qibla. Ndi mchitidwe wa chikristu kutikita mmanja ndi kuyang'ana pa manda mofasa, kapena kupsopsona dothi la pamanda. Zanenedwa mu hadith sharif: **"Munthu akakazonda manda a mbale wake ndi akapereka salaam, mbale wakeyo amazindikira salam yam bale wakeyo.** Ahmad ibni Hanbal "rahima-hullâhu ta'âlâ" states: "Makamadutsa pa manda werengani Ikhlas, ma Sura awiri oyamba ndi Qul-a'udhu..., and Surah Fatiha, ndipo tumizani thawab mwapezazo kwa anthu akufa onweagona kemeneko. Thawb zake zizawapeza." A hadith sharif pogwira mau a Enes bin Malik "rahmatullâhi ta'âlâ 'anh" ikuti: **"Pomwe Ayat-al-kursi ikuwerengedwa ndipo thawab zake aikutumizidwa kwa anthu akufa omwe agona mmanda, Allah Subhana Watala mapangitsa kuti ziwafike onse kumeneko."**

Zanenedwa m'bukhu la **Khazanat-ur-riwayah** lolembedwa Qadi Hindi "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih" "Ngati akatswiri ena amayenderedwa ali ndi moyo, ndizololedwa kuyenda ulendo wa utali kukawazonda atamwalira. Ponena za phindu lopeza, palibe kusiyana pakati pokazonda Atumiki "alaihim-us-salawat-u-wa-t-teslimat" ndi kuzonda Awliya kapena ma Ulama (akatswira a chisilamu) "rahima-hullâhu ta'âlâ". Kusiyana kwawo ndi maudido ndi m gade."

[Ngati msilamu akupachika dzina la munthu amene amamukonda pa khoma la chipinda chake chochezera, kapena kumanga chipilala ndikulemba dzina la muntu ameneyo pa manda ake, nthawi iliyonse

asilamu akulowa mchipidamo kapena kuzonda kumand akapereka salam, Allah Subhana Watala mwini wa dzinalo ndi chifundo chake ndi chikhululuko.

Kulemba dzina pa khoma kapena pa mwala sikutanthauza kumkumbukira mwini wa dzinalo. Zolinga zake ndi zoti Asilamu adzinena Fatih ndi kunena madalitso pa manda potchula mwini dzina. Pachifukwa ichi wasanduka mchitidwe m'mayiko a Chisilamu kulemba mayina pa khoma mzipinda ndi pa zipilala za miyala ku manda. Ngati dzina la Wali lalembedwa, mukawerenga dzinalo ndikupempha mwini wa dzinalo shafaat (kukupemphera chikhululuko) ma dua ndi mdalitso pa iwe, Wali adzakumvani ndipo adzakupemphera kuti pempho ndi zofuna zako zichitika pansi pano ndi kumwamba komwe ndipo mapemphero ake adzavomerezedwa ndi Allah taala.]

Ngakhale kuti kuzonda ku manda ndi kololedwa kwa akazinso, ndikwabwino kuti iwo asakazonde kupatula manda a Rasulullah. Kupita ku manda ali ku msambo (haid) kapena ali ndi Janaba ndi kololedwa koma ndi Sunnah kukhala ndi udhu popita ku manda. Zanenedwa mu hadith sharif: **"Pamene mukukayendera manda a wokhulupirira ndi kunena pephero ili: 'Allahumma inni as-alu-ka bi-haqqi Muhammadin wa ali Muhammadin an la-tu'adh-dhiba hadhal mayyit,' wokhulupirirayo adzapulumutsidwa ku mazunzo.** A hadith sharif ina ikuti: **"Ngati munthu akukazonda manda a makolo ake kapena limodzi mwa makolo kamodzi pa Chisanu, adzapeza chipulumutso."** Ndi zololedwa kupsopsona dothi la pa manda ngati ali manda a limodzi mwa makolo ako. Monga zalongosoledwa m'bukhu lotchedwa **Kifaya**, munthu wana anafunsa Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam": "Ndalumbira kuti ndidzapsompsona khomo la Paradaiso. Ndingakwanilitse bwanji kulumbira kwanga? **"Psompsona phazi la amayi ako,"** anayankha bwana wa atumikiyo. Pomwe munthuyo ananena kuti alibe makolo, Rasulullah ananena: **"Psompson manda a makolo ako! Ngati siukudziwa manda awo, ndiye jambula mizere iwiri kuyimira manda awo ndipo upsompso ne mizereyo! Ukatero wakwanilitsa lumbiro lako."**

Ndibwino kukayendera manda a anthu akuluakulu akutali ndi kwathu tikamapita kumeneko kukachita bizinesi ina, osati kuyenda ulendo wautali ndi cholinga chongokayendera chabe manda awo odalitsika. Koma, zimapatsa thawab zambiri kuyenda ulendo wautali (makamaka) kukamuona manda a Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam". Munthu amene akukayendera manda a Mtumiki "sallallâhu alaihi wa sallam" ndi Awliya alaih-ir-rahma amadalitsika ndi mizimu

yawo yodalitsika. Mtima wake umayeretsedwa mogwirizana ndi chikondi chake ndi momwe akuzigwirizanitsa ndi iwo. Ngati tchimo lichitika pa nthumbira ya Awliya, mwachitsanzo kuti mzimayi wavala mosayenerera wakayenderapo, ichi chusakhale chifukwa choletsera azimayi kukayendera manda a anthu odalitsikawa.

Ngati sitingathe kuletsa kuswa malamulo kotere, tiyenera kudana nawo ndi mtima wonse. Momwemonso, tipite ku maliro a Okhulupirira ngakhale kuli akazi osavala bwino kapena kukuyimbidwa yimbo kapena komwe akuchita maulemu pochita zolankhula.

Ngati kupita ku manda kwa azimayi kuli kokangunguza, kulira kapena kuchititsa fasad (machimo) pophatikizana ndi amuna, ndiye ndi haram. Amayi ochita izi adzudzulidwe. Ngakhale zili zoledwa kuti akazi wokalamba atha kukayendera manda a abale awo kapena a ma Awliya popanda kusakanizana ndi amuna, ndi makruh kwa atsikana achichepere kuyendera manda kotereku. Lamulo lomwelo likugwiranso ntchito kwa azimayi opita ku maliri.

Zanenedwa m'bukhu la **Jila-ul-qulub** lolembedwa ndi Zeyn-ud-din Muhammad bin Ali Birghivi, 928 [1521 A.D.], Balikesir, Turkey–981 [1573] of plague, Birgi): Munthu wolowa ku manda anena: **"As-salamu 'alaikum, ya Ahla dar-il-qawmil-mu'minin! Inna insha-Allahu 'an qaribin bikum lahiqun,"** atayima malo amodzi. Akatha achite Bismillah ndi kuwerenga Sura Ikhlas ka khumi ndi kamodzi (11) kumayamba ndi Bismillah nthawi iliyonse ndiponso Sura Fatiha kamodzi, kuyamba ndi bisimila asanasome surah. Kenako anene dua: **"Allahumma Rabb-al-ajsadil-baliyah, wa-l-izamin nahira-t-illati harajat min-ad-dunya wa hiya bika mu'minatun, eadhil-'alaiha revhan min 'indika wa salaman minni."** Afike pa nthumbirapo atulukira ku manja, bali yak u Qibla kwa mayyit. Ngati koteka kufupi ndi ku miyendo. Apange Salaam, "Salamun 'alaikum." Kaya ayima, agwada kapena akhala, awerenge zigawo zoyamba ndi zomaliza za Sura ya Baqara, kenako Sura Yasin, Sura Tabaraka, Takathur, Ikhlas sharif ndi Fatiha. Atumize thawab zomwe apeza ngati mphatso kwa mayyit.

Mfundo yofunika kwambiri: Akatswiri athu akufotokoza munkhani yochita Hajj m'malo mwa munthu wina kuti ndi kololedwa kupereka thawab yomwe wapeza pochita mapemphero a farz, nafila ndi ntchito zina zopembedza ndi zochita zabwino monga Swalah, kusala; sadaka, kuwerenga Qur'an al-kareem, kupanga dhikr, kupanga tawaf, hajj, umra, kuyendera manda a Atumiki kapena Awliya, kusambisa msilamu wakufa, ngati mphatso ku mzimu wa munthu wina. Anthu onse, amene wachita mapemphero ndi kupereka thawab zake ndi munthu

amene mzimu wake wapatsidwa thawab monga mphatso, onse adzapatsidwa thawab ndi Allahu ta'âlâ. Pachifukwa chimenecho, Qur'an al-kareem iyenera kuwerengedwa mukakazonda ku manda ndi kwina kulikonse ndipo thawab zake ziyenera kuperekedwa kwa mizimu ya okhulupirira akufa. Kenako madalitso ayenera kuperekedwa kwa iwo ndipo ma dua achitike.

Pakuti, rahmat ndi Barakat zimatsika pamalo pomwe Qur'an al-kareem ikuwerengedwa. Mapemphero aliwonse amene angapemphedwe pamalopo amavomerezedwa ndi Allahu ta'âlâ. Ikawerengedwa ku manda, manda amadzadza ndi rahmat (chifundo cha Allahu ta'âlâ) ndi barakah. Malinga ndi Madhhab a Hanafi, Msilamu akuchita ntchito za nafila monga kusala, swalah, sadaka, kuwerenga Qur'an al-kareem kapena kupemphera mapemphero ndikupereka thawab zake kwa Asilamu ena, akufa kapena amoyo, thawab zimenezo zifika kwa Asilamuwo. Akatswili ena a Chisilamu amati lamulo lomweli limagwiranso ntchito pa zopembedza za farz. Thawab sizigawidwa ndi chiwerengero cha mayyits. Thawab zonse zimaperekedwa kwa mayyit aliwonse mopanda kutapa. Malinga ndi ma Madhhab a Maliki ndi Shafi'i, mapemphero omwe amachitidwa mwathupi lokha, monga kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem, sangaperekedwe kwa Asilamu ena. Madalitso amanenedwa pa iwo chifukwa cha ntchito za kuthupi za kupembeza kochitidwa.

Ndipo zalembedwa m'Bukhu la **Kitab-ul-fiqh 'ala-l-medhahibil-erbe'a** kuti: "Kukayendera manda ndi ntchito ya sunnah yochitidwa ndi amuna ndi cholinga chofuna kutenga chenjezo kuchokera kwa anthu akufa ndi kusinkhasinkha za moyo wakudza. M'Madhhab a Hanafi ndi Maliki, ndi sunnah muakkad kukazonda kumanda Lachinayi, Lachisanu kapena Loweruka. Mu Madhhab a Shafi'i ndi sunnah muakkad kuyendera pakati pa masana Lachinayi ndi kutuluka kwa dzuwa Loweruka. Wokazondayo awerenge kapena alakatule Qur'an al-kareem kwa mayyit ndi kuwadalitsa. Zinthu izi zidzakhala zothandiza kwa mayyit. Mukafika ku manda, ndi sunnah kunena pemphero ili: "**As-salamu 'alaikum, ya Ahla dar-ilqawm-il-mu'minin! Inna insha-Allahu 'an qaribin bikum lahiqun.**" Manda aliwonse amayenderedwa akutali ngakhale a pafupi. Ndipo ndi sunnah kuyenda mtunda wautali ndi cholinga choyendera a silamu a Salih ndi ma Wali "rahima-hullâhu ta'âlâ".

Amodzi machitidwe opembedzera ofunika kwambiri kupita ku manda odalitsika a Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam". Kukayendera ku manda ndikololedwanso kwa azimayi okalamba,

pokhapokha atavala moyenera. Ndi haram kwa azimayi okalamba ngati zitayambitsa fitna ndi fesad. Ndi kosaloledwa kuchita tawaf mozungulira manda kapena kupsompsona nthaka kapena kupempha china chake kwa akufa pa ulendowo." Awliya "rahima-hullâhu ta'âlâ" amapemphedwa shafa'at, kaamba ka chiombolo cha madalitso a Allahu ta'âlâ.

Pali zinthu ziwiri zomwe zikusowa,
Zidzawotcha zonse, mosalabadira kuti ndi ndani.
Maso okhetsa mwazi sadzawabwezera mangawa ao;
Mmodzi ndi wachinyamata, wina: M'bale wa chisilamu!

BUKHU LACHITATU
KALATA YA CHISANU NDI CHINAYI (9)

Kalata ya chisanu ndi chinayi ya bukhu la chitatu lotchedwa 'Maktubat' lolembedwa ndi Imam Rabbani Mujaddid-i-elf-i-thani Ahmad Faruqi "rahima-hullâhu ta'âlâ", kulembera Mir Muhammad Nu'man. Bukhuli likofotokoza za ayat-karima yomwe ikuti: "Tengani zomwe Rasulullah wakubweretserani!" Kalatayi ili mchiyankhulo cha chi Arabu ndipo Chichewa chake chili motere:

Bism-illah-ir-Rahman-ir-Rahim! Ayah ya chisanu ndi chiwiri (7) ya karima Sura Hashr ikuti: "ndipo chimene wakupatsani mtumiki, chilandireni; ndipo chimene wakuletsani chisiyeni, muwopeni Allah!"

[Kuchita zomwe zavomerezedwa ndi kupewa zoletsedwa, pamozi zimatchedwa kumvera Chisilamu] Allahu ta'âlâ ponjezera mau oti "muwopeni Allah" kumapeto koti "chimene wakuletsani chisiyeni …," kukusonyeza kuti ndikofunika kwambiri kusiya zoletsedwa. Chifukwa kuopa Allahu ta'âlâ, yomwe ndi taqwa, zimathandauza kupewa zoletsedwa (za haram). Taqwa ndiye maziko a Chisilamu. Kupewa zochitika zokayikitsa kumatchedwa 'wara'. Rasulullah "sallallâhu alaihi wa sallam" ananena: "Wara' ndi mzati wa chipembezo chathu" Ananenanso mu hadith sharif: Palibe chingafanane ndi wara" Chipembezo chathu chikulimbikitsa kufunika kopewa za haram chifukwa cha kuchuluka kwa zochitika zofunika kuzipewa choncho ndi kofunika kwambiri kupewa za haram. Pakuti, kuchita lamulo kulinso ndi mbali yopewa. Kuchita lamulo lina lake kumatanthauza kupewa kusachita lamulolo. Ndipo kukhala kothandiza kwambiri ndi kukhala kutsutsana ndi kusasunthika kwa ma nafs. Ndipo kuti zikhale zofunika, kutengera kugonja motsutsana ndi nafs. Pamene lamulo likuchitidwa,

nafs imakhalanso ndi gawo kuchokera ku chisangalalo chopezeka. Pamene chilakolako chikuchepetsedwa pochita chinthu, ndi pomwe padzafunike kwambiri kuchita chinthucho. Kunena zoona, zizakuthandizani inu kupeza chisomo cha Allahu ta'âlâ mwachangu. Pakuti, Ahkam-i-islamiyya, (malamulo ndi zoletsa za Chisilamu), cholinga chake ndi kupondereza ndi kunyozetsa nafs. Nafs ndi mdani wa Allahu ta'âlâ. Kwanenedwa mu hadith qudsi kuti: "Mudane ndi ma nafs anu! Pakuti, ndiye mdani Wanga." Choncho, mwa turuq-i-'aliyya (njira ndi malamulo a Tasawwuf), omwe amaphunzitsa kumvera kwambiri Chisilamu ndi amene adzawongolera kuyandikira kwa Allahu ta'âlâ. Pakuti, amenewo amatsutsana kwambiri ndi nafs. Ndipo izi, monga zikudziwikira ndi odziwa bwino nkhaniyi, ndi njira yomwe takhala tikutsata. Ndi chifukwa chake katswiri wina wozama kwambiri, Behaaddin Bukhari, yemwe ndi mtsogoleri wathu wamkulu, ananena kuti: "Ndapeza njira zazifupi kwambiri zimene zimachititsa munthu kupeza Allahu ta'âlâ." Pakuti, njira iyi imalangiza kutsutsa kwambiri ma nafs. Chifukwa cha kupambana kwa njira iyi pokwimitsa kumvera chisilamu, zidzakhala zosavuta kwa munthu wanzeru komanso wololera yemwe akuwerenga mabuku olembedwa ndi atsogoleri athu kuti azindikire izi.

Munthu ameneyo adzaona mfundoyo bwinobwino. Chowonadi chomveka bwino momwe chilili, ndafotokoza mwatsatanetsatane m'makalata anga angapo. Allahu ta'âlâ akudziwa chowonadi cha chilichonse. Thandizo lakelidzatikwanira. Iye ndi wowerenga wabwino kwambiri. Swalah (mapemphero ndi madalitso) ndi salam (mapemphero, malonje, chipulumutso) kwa Mbuye wathu Muhammad "alaihim-salâm" kwa Aku banja lake ndi Ashab "radiyallâhu ta'âlâ 'anhum ajma'in", ndi kwa anthu otsatira njira yabwino!

BUKHU LA CHITATU, KALATA 84

Hamd (matamando ndi kuyamika) zikhale kwa Allahu ta'âlâ, ndipo salaam kwa akapolo Ake amene anawasankha ndi kuwakonda! Munthu amene akufuna kulimbikira m'njira imeneyi ndi kupeza chikondi cha Allahu ta'âlâ, akuyenera kuyamba ndi kukonza chikhulupiliro chake molingana ndi ziphunzitso za akatswiri a njira yolondola, a Ahl sunnat. [Akatswiri ozama awa anapeza maphunziro awo onse kuchokera kwa Ashab kirim.

Asasokonezedwe ndi maganizo awo kapena maganizo a akatswiri a nzeru za pamwamba.] Allahu Subhana Watala adalitse anthu

opambanawa ndi zochuluka kapena malipiro ogwirizana ndi ntchito zawo! Kenako munthu ameneyo ayenera kuphunzira chidziwitso cha Fiqh chomwe ndi chofunika kwa munthu aliyense. Kenako, ayenera kugwiritsa ntchito zomwe waphunzira. Pambuyo pake, apange dhikr kwa Allahu Subhana Watala nthawi yake yonse. [Nthawi zonse ayenera kumaganizira za Allahu ta'âlâ ndi Zizindikiro zake zotchedwa Sifat-i-dhatiyya.] Koma kupanga dhikr kumasowekera kuphunzira kaye kachitidwe kake kuchokera kwa munthu wodalitsika yemwe ali kamil ndi mukammil, [Kamil ndi munthu amene wakwaniritsa ungwiro motsogozedwa ndi munthu wina wapamwamba ndi wodalitsika. Mukammi ndi munthu yemwe walolezedwa ndi omuphunzitsa ndi kumuongolera wake wamkulu okhala ndi ijazat [diploma] kuti awaongole Asilamu ena ku ungwiro.] Ngati akuphunzira kuchokera kwa ma sheikh osaphunzira komanso ongoganizira chabe, sangapeze ungwiro. Koyamba ayenera kupanga dhikr kwambiri; kotero kuti akatha kuswali swalah iliyonse mwa swalah zisanu za fardh za pa tsiku ndi tsiku ndi ma sunnah, asachite zopembedza zina koma dhikr. Ngakhale kuwerenga kapena kulakatula Qur'an al-kareem ndi machitidwe ena opembedza a nafila azisiye mpaka nthawi ina. Dhikr ipangidwa muli ndi udhu ngakale mulibe. Ntchito imeneyi iyenera kuchitika mosalekeza, poima, pokhala pansi, poyenda, ndiponso pogona. Pasadutse mphindi ngakhale imodzi osachita dhikr pomwe mukuyenda munseu, podya ndi pogona. Mizere iwiri ya chi Persia m' Chichewa:

Pangani dhikr, moyo wanu wonse, nthawi zonse, Pali ponse!
Ndi dhikr yokondedwa, mtima woyera, palibe njira zina.

Dhikr ichiteke mochuluka, pasakhalenso khumbo lina kapena lingaliro lina kuposa kuchita dhikr, Allahu ta'âlâ. Zisasiyidwa mu mtima mwake. Mumtima mwake musakhale mayina azinthu zina ngakhalenso zizindikiro zina koma dzina la Iye. Ngakhale atadzikakamiza kuganiza zinthu zina osati Iye, ayenera kulephera kuzisunga kumtima kwake. Kusiya kuzindikira zinthu zina ndi kuzindikira Allah taala yekha uku ndi ndi chiyambi chopeza mwayi waukulu. Kuleka uku ndi nkhani yabwino yopeza chisomo ndi chikondi cha Matlub (Allahu ta'âlâ). Mizere iwiri ya chiarabu m'Chichewa:

Kodi tingafikire bwanji Su'ad yapambamba,
Ndi mapiri atali ndi magwero akuya pakati!

[Su'ad ndi dzina la ma'shuqa (wokondedwa).] Allahu ta'âlâ, yekha ndi amene amapangitsa munthu kupeza chilichonse. Salaam kwa

anthu omwe ali pa ulendo mu njira ya chiongoko! [Zanenedwa m'kalata ya chikhumi ndi chisanu ndi chiwiri (17) m'buku lachitatu: "Kupanga dhikr ndi mtima kumam'masula munthu ku zinthu zina zosakhala za Allahu ta'âlâ. Kukonda kwa mtundu uwu ndi matenda a mtima. Pokhapokha ngati mtima utachoka ku matendawo, munthu siwungapeze iman yoona ndipo zidzakhala zovuta kumvera Ahkami-islamiyya, omwe ndi malamulo ndi zoletsedwa za Allahu ta'âlâ. Imakhalanso dhikr kupanga niyya yomvera malamulowa ndi kusaganiziranso zokhudza nafs pochita ma mubah (zilolezo)." Matenda a mtima ndiye kutsatira nafs. Nafs ndi mdani wa Allahu ta'âlâ. Sikufunaka kuyimvera. Ndi mdani pa yekha. Nafs zichititsa mtima kumva kokoma zomwe zimapangitsa ziwalo zonse kuchita zoipa komanso kuchita zinthu zoononga. Nafs zimafuna kukhala zosapembedza komanso zopanda Iman kuti zipeze zosangalatsa izi. Zimapereka matenda ku mtima wopanga ubwenzi ndi anthu osakhulupirira ndi anthu opanda Madhhab powerenga mabuku ndi nyuzipepala zao, kumvetsera ma pulogalamu awo a pawailesi ndi kuonera kuulutsa kwawo koipa kwa wailesi yakanema. Chomwe chimachiritsa matenda a mtima ndi kumvera Chisilamu. Kumvera Chisilamu kumadwalitsa Nafs. Chisilamu chimachepetsa zokondweretsa za nafs, zilakolako zake ndi mphamvu yake yokhudza mtima.]

Ndani amapambana pa dziko lapansi po kukwaniritsa zokhumba zawo?
Ndithu, chilichonse chili m'tsogolo chimachitika!

KALATA YA 114

Pali makalata zana limodzi ndi makumi awiri ndi asanu (125) m'bukhu lotchedwa Makatib sharifa. Bukhuli ndi lolembedwa ndi Abdullah Dahlawi "rahima-hullâhu ta'âlâ", m'modzi mwa akadaulo akulu kwambiri ku India. Zotsatirazi ndi zolembedwa za Chichewa za kalata ya zana limodzi ndi khumi ndi chinayi (114), yomwe inalembedwa kwa Haji Abdullah Bukhari:

Palibe chosowa mwa Allahu ta'âlâ. Nthawi zonse amanena zoona, ndipo amawasonyeza njira yoongoka akapolo Ake. Salaam zathu ndi mapemphero athu akhale pa mtsogoleri wathu wapamwamba kwambiri komanso wokondedwa Muhammad Mustafa "sallallâhu alaihi wa sallam", ku banja lake lodalitsika ndi kwa Ashab (ma swahaaba) "radiyallâhu ta'âlâ 'anhum ajma'in"! Amuna aku Tariqa omwe akukhala kuno, [mu mzinda wa Delhi,] akuwerenga Esma ndi

kulemba ma musqa (zithumwa) ndi cholinga chokwaniritsa zokhumba zawo. Potero anthu ena amakopa ndi iwo. Iwo akutenga Emir-ul-mu'minin Ali 'karrim-Allahu wajhah wa "radiyallâhu ta'âlâ 'anh" kukhala wapamwamba kuposa ma Khalifa eana atatuwa "radiyallâhu 'anhum" . Anthu amenewa amatchedwa ma Shi'a. Anthu amene amadana ndi ma Khalifa atatu enawa ndi Ashab-i-kirim amatchedwa ma Rafidi.

[Akatswiri a **Ahl sunnah wa-l-jama'at** "rahima-hullâhu ta'âlâ" anena m'mabuku awo osiyanasiyana kuti Hadrat Abu Bakr, Hadrat Umar ndi Hadrat Uthman ndi opambana kuposa Hadrat Ali "radiyallâhu ta'âlâ 'anhum ajma'in", ndipo anatsimikizira mfundo imeneyi popereka umboni wochuluka ku ayah karima, ku ma Hadith sharif ndi ku ijma, yomwe ndi migwirizano ya Ashab Kiram "radiyallâhu ta'âlâ 'anhum ajma'in".

Awiri mwa mabuku ofunikawa ndi **Izalat-ul-khafa 'an khilafat-il-khulafa** ndi **Qurrat-ul-'aynain** fi tafdhil-i-shaikhayn, onse olembedwa ndi Waliy-yullah Muhaddith Dahlawi "rahima-hullâhu ta'âlâ" (1114 [1702 AD] - 1176 [1762], Delhi). Mabukuwa ali wolembedwa m'zinenero za Chiarabu ndi Chipersia mosakaniza. Bukhu loyamba linamasuliridwa m'chinenero cha Chiurdu ndipo ma bukhu a ziyankhulo ziwiri zonse anasindikizidwa ku Pakistan mu 1382 [1962 A.D.]. Bukhu lachiŵiri linamasuliridwa m'Chituruki ndipo kenako m'Chingelezi. Bukhu la chingelezi latenga mbali yaikulu ya gawo lomaliza la bukhu lotchedwa Sahaba 'The Blessed', limodzi mwa zofalitsidwa za Hakikat Kitabevi ya ku Istanbul, Turkey. Lilinso ndi gawo mu bukhu lotchedwa 'Documents of the Right Word'. Bukhu la chiarabu lotchedwa **Es-sawaiq-ul-muhriqaand** lolembedwa ndi katswiri wamkulu wa chisilamu Ibni Hajar-i-Makki "rahima-hullâhu ta'âlâ" (899 [1494 AD] - 974 [1566], Makka) linapangidwanso mwa njira yochotsera ku Istanbul, Turkey, ndi a Hakikat Kitabevi. Msilamu womvetsa yemwe angawerenge bukhu limeneli adzazindikira mosavuta kuti anthu opanda madhhab akutsata njira yolakawika. Ena mwa anthu amenewo akudzitcha kuti ndi Ja'fari mpaka lero. Akumanamiza achinyamata ndi bodza loti iwo ndi otsatira a ma Imam khumi ndi awiri. Koma zoona ndi zoti Asilamu omwe amatsatira ma Imam khumi ndi awiriwo amatchedwa asilamu a Ahl Sunna. Akatswiri a njira yoona otchedwa Ahl sunnah "rahima-hullâhu ta'âlâ" anena kuti: "Kukonda ma Imam khumi ndi awiri kudzachititsa kuti Msilamu afe limodzi ndi iman."

Akukonzekera mwambo wa maliro ndi ma pwando ndi cholinga choyimba ‘dawr’. [Saswali swalah mu jama’ah. M’mizikiti ndi m’misonkhano ya Maulidi ali ndi magulu omwe oyimba Ilahis (zotamanda wakufa) ndi marsiyas (zotamanda Imam Hussain). Iwo akumvetsera zida zoimbira monga ma banjo a ku komventi (nyumba za masisitere). Akuchita bid’ah ndi zina zambiri zopeka m’dzina la Tariqat (Njira za Tasawwuf). Ponena zoona, akuwonjezera zichitochito zosakhala zachipembedzo za ma Jukism ndi Brahmanism mu zomwe amazitcha Tariqat. Amakhala paubwenzi ndi anthu otsata zabwino zapadziko lapansi ndi anthu a fasiq (ochimwa). Salabadira za qawma ndi jalsa mu Swalah ya jama'at, ndi swalah ya Lachisanu, (zomwe zafotokozedwa kale mwatsatanetsatane m'bukhu lino). Zichitochito ndi miyambo yawo mu Chisilamu mulibe. Zinthu zimenezo kunalibe mu nthawi ya Salaf-assalihin. Akatswiri a maphunziro a **Ahl sunnat wa-l-jama’at** “rahima-hullâhu ta’âlâ” adapewa machitidwe ndi njira za bid’at zotere. Tithokoze Allahu ta’âlâ, kuti machitidwe oipawa wa bid’at ngati uwu palibe pakati pa Ashabi-kiram “radiyallâhu ta’âlâ ’anhum”. Munthu amene akufuna kukhala Msilamu ndi kutsatira mapazi a Salaf-as-salihin (akatswiri akale achisilamu) “rahima-hullâhu ta’âlâ” awatalikire anthu onyenga otere a Tariqat. Iwo ndi mbava za chikhulupiriro. Iwo akuwononga chipembedzo ndi Iman ya akapolo a Allahu ta’âlâ. Ma dhikr awo ndi machitidwe ena amayambitsa mtima ndi nafs zawo kuyamba kuyenda. [Zinthuzi ziyenera kuyeretsa mtima ku ma-siwa (maganizo osakhala a Allahu ta’âlâ) osati kusokoneza zinthu ndi zochita zina.] Komanso zinthu monga kashfs [karamat, zochita zozidzitsa ndi kuulula zinthu zosowa ndi kuyankhulana ndi mizimu] zilibe phindu m'Chisilamu. Anthu osakhulupirira monga ma Juki nawonso amachita ndi kuonetsa ma kashf ndi makaramats. Anthu anzeru ayenera kukhala tcheru ndi kutha kusiyanitsa pakati pa chabwino ndi choipa. Kukhulupirira Chisilamu ndi kukonda za dziko lapanso ndi zinthu ziwiri zotsutsana zomwe sizingakhale pamodzi mwa munthu. Munthu wa nzeru sanganyengereredwe zosiya nsichi za chipembedzo chake ndi cholinga chofuna kupeza zinthu za m’dzikoli. Akatswiri ndi ma sheikh a mumzinda wa Bukhara anali anthu a tawakkul (kukhulupirira mwa Allahu ta’âlâ). Sanali okonda za bwino za dziko lapansi. Kupanga ma phwando ndi kusonkhanitsa anthu okonda za pa dziko lapansi kumadetsa mtima wa munthu. Anthu afunikira amenewo ankapewa zinthu ngati zimenezi. Iwo anamatirira chikhulupiriro cholondola chophunzitsidwa ndi Salaf-i-salihin “rahima-hullâhu ta’âlâ” ndi ma sunnah a Rasulullah “sallallâhu alaihi wa sallam”. Mu chilichonse amachita, ankakonda njira ya **Azimat**. Iwo ankapewa za bid’ah. Ankapewa zinthu

zobwera m'njira za har'am kapena makruh. Pamene mubahs (zilolezo) zikuyambitsa za haram, izonso zimakhala za haram.

Dhikr-i-khafi, dhikr ya mu mtima ndi bwino kuposa **dhikr-i-jahri**, (kupanga dhikr mokweza). Iwo ankachita Dhikr-i-khafi. Iwo anali atapeza mulingo wa 'ihsan' watchulidwa mu hadith sharif. Nthawi zonse mitima yawo imatembenukira ku gwero la fayz, [Allahu ta'âlâ.] Ngati wokhulupirika ndi wodzipereka atapeza tawajjuh ya munthu wapamwamba wa Tasawwuf, mtima wake, ndi ma latifa ake onse, nthawi yomweyo amayamba kuchita dhikr. Adzapeza hudhur, mtima osalabadira chilichonse koma Allah Ta'âlâ, zomwe zimatchedwa **mushahada**, jadhbas ndi ma fayze otchedwa **waridat**, omwe ndi madalitso amene wodzipereka amasamba mu nurs mu zahir (kunja kwake, m'thupi) ndi mu batin wake (mkati, uzimu). Wodzipereka akayamba kulandira fayz kuchokera mu mtima mwa murshid, palibe lingaliro lililonse kupatula la Allahu ta'âlâ lomwe lidzafike pamtima pake. Ziwalo zake zonse zidzayamba kuchita mogwirizana ndi Sunnat ndi azimat. Azakhala m'chisangalalo chachikulu odalitsika amenewa. Ya Rabbi! Chifukwa cha chisomo cha Wokondedwa Wanu Mtumiki Muhammad Mustafa "sallallâhu alaihi wa sallam" ndi chisomo cha mashaikh kirim "rahmatullâhi ta'âlâ 'alaih ajma'in", omwe ndi otsatira a Mneneri wolemekezeka ameneyo, chitani izi kukhala chakudya chathu codalitsika cha tsiku ndi tsiku. Ma Fayze a Imam Rabbani mujaddid-i-alf-i-thani "rahmatullâhi 'alaih" pangani kuti ma latifa a munthu apeze madalitso amenewa.

Moyo wanga uperekedwe nsembe m' njira yanu,
Kukongola mu'dzina lenileni, Muhammad!

Chonde mpembereren kapolo wanu wodzichepetsa,
Kukongola mu'dzina lenileni, Muhammad!

Okhulupirira amavutika kwambiri m'moyo uno,
Adzalipidwa m'moyo winawo.

Chisankho cha maiko zikwi khumi ndi zisanu ndi zitatu m'moyo,
Kukongola mu'dzina lenileni, Muhammad!

Yemwe akuyenda m'mithambo isanu ndi iwiri,
Yemwe akuyenda pamwamba pa Kursi ndi thambo,

Yemwe akupemphara Haqq Umma wake ku Mi'raj,
Kukongola mu'dzina lenileni, Muhammad!

Ndi a chani maiko awiri kwa Yunus, popanda inu?
Mopanda kukayika konse, ndinu Mneneri woona!

Anthu okanira za inu, akudutsa popanda Iman;
Kukongola mu'dzina lenileni, Muhammad!

MFUNDO ZOTSIRIZA KUCHOKERA M'BUKU LA NJIRA YOPITA KU PARADISO

Timaona kuti zinthu zonse, zamoyo ndi zopanda moyo mofanana, zonse zili mwadongosolo. Timaphunzira kuti pali dongosolo losasinthika ndi mgwirizana wamasamu mkupanga kwa chinthu chilichonse, muzochitika zilizonse, pakuchita kulikonse. Timagawa makonzedwe ndi kulumikizana uku m'magulu monga malamulo a physics, chemistry, astronomy, biology, ndi zina zotero. Pogwiritsa ntchito dongosolo losasinthikali, timapanga makampani, timatsegula mafakitale, timapanga mankhwala, timapita ku mwezi, ndi kukhazikitsa kugwirizana kwa nyenyezi ndi ma atomu. Timapanga ma wailesi, ma televishoni, makompyuta, ndi ma network. Pakanapanda dongosolo ili la zolengedwa, bwenzi chilichonse chiri cha chisawawa, sitikanayendetsa chilichonse mwazinthu izi. Zinthu bwenzi zikungogundana, bwenzi palibe dongosolo, ndipo ngozi ziri zambiri. Zonthu zonse bwenzi zitatha.

Kukhazikika kumeneku, kutsata dongosoloku ndi kulumikizana pakati pa zolengedwa, kukuwonetsa kuti sizinakhaleko zokha kapena mwamwayi, ndikuti chilichonse chinalengedwa ndi wodziwa zonse, wamphamvu zonse, wopenya ndi wakumva zonse amene amachita chilichonse chomwe akufuna kuchita.

Iye amalenga ndi kuwononga chirichonse mwa kufuna kwake. Amapanga zinthu zoyambitsa ndi njira zopangira kulengedwa kwa zinthu zina. Akandalenga popanda zoyambitsa ndi njira, sipakanakhala dongosolo lokhazikika pakati pa zolengedwa. Chilichonse chikanakhala mchipwirikiti. Sipakanakhala zizindikiro zosonyeza kukhalapo Kwake. Bwenzi kulibe malaonda, sayansi kapena kutukuka pa umoyo.

Sanangoonetsera kukhalapo Kwake kudzera mu dongosolo ili, komanso adalengeza za kukhalapo Kwake kwa akapolo Ake, zomwenso zimasonyeza ukulu Wake kwa akapolo Ake. M'zaka 100 zilizonse, kuyambira ndi Adam "alaihim-salâm", anasankha munthu m'modzi kuchokera m'madera onse pa dziko lapansi, ndikumolenga kukhala wabwino kwambiri komanso wa pamwamba kwambiri pakati pa anthu ake. Amamutumizira mngelo Wake, kudzamudziwitsa za

kukhalapo kwake ndi Mayina Ake, ndipo kumulangiza zomwe anthu ayenera kuchita ndi zomwe ayenera kupewa kuti akhale ndi moyo wabwino ndi wotokoza padziko lapansi ndi tsiku lomaliza. Anthu osankhidwa amenewa ndi apamwamba amenewa amatchedwa **Atumiki.** Malamulo ndi zoletsedwa zomwe adapereka kwa anthu zimatchedwa **Din** (chipembedzo) ndi **Ahkam diniyya** (malamulo achipembedzo). Poti ndi chibadwa cha munthu kuyiwala za kale, ndipo kuti anthu oipa amene nthawi zonse amakhalapo pakati pa anthu, ali nako kuthekera kowerenga mabuku a Atumiki alaihim-us-salawat-u-wa-t-teslimat ndi kusintha zolankhula zawo, zipembedzo zakale zayiwalika ndikudetsedwa.

Choipa kwambiri ndi chakuti anthu oipa apanga ndi kupeka zipembedzo zabodza. Poti Allahu ta'âlâ, Mlengi wa zonse, amamvera kwambiri chisoni anthu, Iye watumizira Mneneri womaliza ndi chipembedzo chatsopano. Ndipo wawauza nkhani yabwino yoti IYE adzachiteteza chipembedzochi mpaka kumapeto kwa dziko lapansi ndikuchifalitsa kutali ngakhale kuti anthu oipa akuukira ndi kuyesayesa kusintha ndi kuchidetsa.

Kuthokoza kwathu ndi kwakukulu kwa Allahu ta'âlâ kuti takhala tikukhulupirira kuti Mlengi alipo ndipo ndi m'modzi kuyambira tili ana ang'ono. Tinapezanso mwayi wodziwa kuti dzina la Mlengi ameneyu ndi Allah, zoti kuti Muhammad "alaihim-salâm" ndi Mneneri wake womaliza, ndipo **Chisilamu** ndi chipembedzo chimene Mtumiki wokondedwa uja adafikitsa kwa akapolo Ake, (anthu.) Tikufuna tiphunzire chipembedzo cha Chisilamuchi molondola. Mu zaka zonse za maphunziro ku sukulu yasekondale ndi ku yunivesite, tinafufuza komwe tingaphunzire. Koma achinyamata amtundu wathu anali atazunguliridwa ndi chotchinga chomwe sichingagonjetsedwe chomwe ndi anthu a sayansi abodza omwe anadzikoletsa okha ku ma freemason ndi ma kominisimti ndi aganyu omwe adatengeka ndi ma wahhabi kukhala achipembedzo chopanda Madhhab aliwonse. Mokakamira kwambiri ntchito zanseli zinachitika ndi anthu a oupandu amene anasinthanitsa chikhulupiriro chawo pogulitsa ndi zinthu za dziko lapansi kotero kuti kunali kosatheka kulinganiza njira yolondola yozisiyira. Panalibe njira yotulukira kuposa kupempha kwa Allahu ta'âlâ. Allah wathu, wapamwambamwamba, watidalitsa ndi kuwerenga mabuku olembedwa ndi akatswiri a maphunziro a Ahl sunnat "rahima-hullâhu ta'âlâ". Koma kukhudzika komwe tinali nako m'dzina la chidziwitso cha sayansi ndi asayansi amatsenga omwe odzitchula kuti ndi anthu amakono komanso m'dzina lo tanthauzira

Qur’an al-kareem ndi anth achipembezo onyenya omwe omwe akugwiritsa ntchito Chisilamu pokwaniritsa zofuna zawo zinali zitalowa mkati mwa moyo wathu.

Kuthokoza kopanda malire kukhale kwa Allahu ta’âlâ potidalitsa ndi kudzutsidwa chifukwa cha machenjezo a amuna achipembedzo achilungamo, kotero kuti tinayamba kusiyanitsa pakati pa chabwino ndi choipa. Tinatha kuzindikira kuti zimene zinadzadza m’maganizo mwathu zinali poizoni m’malo mwa chidziwitso. Mitima yathu unadetsedwa ndi zotsatira zake zoipa. Kupanda kuti tinaona mabuku olembedwa ndi akatswiri a Ahl Sunnah, tikanalephera kusiyanitsa pakati pa a bwenzi ndi adani, ndipo tikananyedwa ndi ziwembu ndi mabodza a m'mitima ya anthu omwe ndi adani a chipembezo. Sitikanatha kuthawa kuchokera ku misampha yoikidwa ndi adani obisika amenewo amene akhala kunena za kusapembedza ndi ‘kupita patsogolo chiwerewere.

Tikanakhala tikunyoza makolo athu, Asilamu owona ndi oyera, ndi ziphunzitso za chisilamu zomwe tinaphunzira kwa iwo. Mtumiki wathu wokondedwa “sallallâhu alaihi wa sallam” akutichenjeza za kugwa mu misampha imene adani a Chisilamu amaika: **“Phunzirani chikhulupiriro chanu kuchokera mkamwa mwa rijal!** Tikapanda kumupeza rijal aliyense, monga akatswiri wa chipembedzo owona, tidzaphunzira kuchokera ku mabuku awo. Mabuku achipembedzo olembedwa ndi anthu a bid’ah kapena anthu osaphunzira a chipembedzo, opanda Madhhab ena ndi owopsya kwambiri ngati mabuku olembedwa ndi osakhulupirira.

Ndi haramu kwa azimayi ndi atsikana kuonetsa poyera mitu yawo, tsitsi, mikono ndi miyendo yawo. Amuna asaonetsa mbali ya matupi awo pakati pa michombo ndi mawondo awo pamaso pa ena. Allahu ta’âlâ wawaletsa izi. Madhhab anayi oona, amene amaphunzitsa malamulo ndi zoletsedwa za Allahu ta’âlâ, amasiyana wina ndi mzake m’nkhani zawo za ma awrat a anthu, mwachitsanzo, ziwalo zawo amuna sayenera kuonetsa kwa ena kapena kuona za ena. Msilamu aliyense akuyenera kuphimba mbali zake za awrat zomwe zafotokozedwa ndi Madhhab omwe alimo. Zili haram ena kuwona mbali zake izi ngati zaonekera. M’buku lamutu wakuti **Kimya-i-se’adet** zanenedwa kuti: “Ndi zoipitsitsa kwa akazi ndi atsikana kuti si kusaphimba kokha kwa mitu, tsitsi, mikono ndi miyendo, komanso sayenere kuvala madiresi owonekera mkati, okongoletsedwa, othina ndi onunkhira. Ngati makolo awo, amuna awo ndi abale awo akuwalola kutero, kuvomereza kutero ndi kuwalekerera, iwo

adzagawana nawo tchimo lawo ndi chizunzo chimene adzalangidwa nacho.” Iwo adzazunzidwa pamodzi kumoto wa Jahannama. Akachita tawba, adzakhululukidwa ndipo sadzatenthedwe. Allahu ta’âlâ amakonda anthu ochita tawba. Munali m’chaka cha chitatu cha Hijra pomwe atsikana omwe adakwanitsa zaka zozindikira ndi kutha msinkhu komanso akazi analetsedwa kudziwonetsera kwa amuna omwe ndi na-mahram kwa iwo. Sitiyenera kukhulupirira bodza la kuti kudziphimba kwa akazi kunayamba pambuyo pena pake ndi akatswiri a Fiqh. Ndi chinyengo cha akazitape a ku Britain ndi anthu ena osaphunzira omwe ogwiritsidwa ntchito ndi iwo pofalitsa bodza lofotokoza kuti akazi samadziphimba kusanavumbulutsidwe ayah yolamula hijab (kuphimba akazi ndi atsikana). Tikunenanso: Mwana akayamba kukhala aqil (wanzeru) ndi baligh (kutha msinkhu), ndiye kuti wafika msinkhu wolekanitsa zabwino ndi zoipa ndikulowa m'banja, zimakhala farz kwa mwanayo, nthawi yomweyo phunzirani mfundo zisanu ndi imodzi za iman (chikhulupiriro) ndipo pambuyo pake aphunzire **Ahkam islamiyya**, zomwe ndi ma farzes, ma halal ndi ma haram, ndikukhala moyo wotsatira malamulo ndi mfundozi.

Mtsikana amakhala aqil ndi chisangalalo akafika zaka zisanu ndi zinayi, ndipo mnyamata amakhala chomwecho ali ndi zaka khumi ndi ziwiri. Zimakhala farz kwa iwo kuphunzira mfundo izi, malamulo ndi mfundo pofunsa makolo awo, anzake ndi achibale, ndi abwenzi.Chimodzimodzinso kafiri amene walowa m’Chisilamu, ayenera kupite nthawi yomweyo kwa munthu achipembedzo, kwa mufti, ndi kukaphunzira kwa iwo. Ophunzitsa naye ayenera kumuphunzitsa munthuyo mwachindunji kapena pomupatsa chisilamu chenicheni. Amupatse bukhu ngati mphatso. Ndi farz kuti mbali zonse ziwiri zichite mbali yawo, kutanthauza kuti Msilamu watsopanoyo aphunzire, ndi kuti munthu wofunsidwa amuthandize kuphunzira. Ngati gulu lomalizali lingonena kuti, “Zabwino kwambiri, zabwino kwambiri,” ndipo osawathandiza powaphunzitsa kapena powapatsa mabuku oona achisilamu, ndiye kuti aphwanya lamulo (lalamulo lotchedwa) farz. Munthu amene samvera Farz adzazunzidwa kumoto wa Jahena. Munthu wolowa kumene chisilamu akayamba kufunafuna munthu wachipembedzo kapena buku lachipembedzo, idzakhala 'udhr kwa iye kuti asaphunzire ziphunzitsozo mpaka atapeza magwero a chiphunzitsocho. (Udhr ndi chinthuchomwe chimamulepheretsa Msilamu kuchita lamulo lachisilamu kapena kupewa choletsa cha Chisilamu. Poti malamulo ndi zoletsedwazi zakhazikitsidwa ndi Chisilamu, momwemonso ma 'udhr pa malamulo onse achisilamu ndi Zoletsa zakhazikitsidwanso ndi Chisilamu. Monga

gwero la kuphunzira malamulo ndi zoletsa za Chisilamu olembedwa m'mabuku a akatswili a Ahl sunnat, momwemonso ma 'udhrs atha kuphunziridwa kuchokera kwa akatswiri a Ahl sunnat kapena m'mabuku awo. Hakikat Kitabevi ya ku Istanbul, Turkey, ndi dipatimenti yosungira chuma cha Chisilamu masiku ano komwe munthu angapeze mabuku onse ofunikira m'zinenero zosiyanasiyana.)

Pofuna kuti mibado yachichepere imve za ziphunzitso zoona za chisilamu zomwe tawerengaza ndi kutumikira anthu onse pa dziko lonse lapansi kuti apeze chitonthozo ndi mtendere pa dziko lapansi ndi chisangalalo chosatha pa tsiku lomaliza, insha-Allah, tidzapitiriza ntchito yathu yosindikiza ma bukhu osankhidwa ndi zolemba za mtengo wapatali zochokera m'mabuku olembedwa ndi akatswiri a Ahl sunnat.

Pemphero lotsatirali, lotchedwa **Salat-an-tunjina**, liwerengedwe pofuna kukwaniritsa zofuna: "Allahumma salli 'ala sayyidina Muhammadin wa ala al-i-sayyidina Muhammadin salat-an-tunjina biha min jami'ul ahwal-i-wa- l-afat wa taqdi lena biha jami'al hajat wa tutahhiruna wa tuballighuna biha min jami' is-seyyiat wa terfe'una biha a'l-ad-derejat wa tubellighuna biha aqsa-l-ghayat min jami'il khayrat-i-fi-l-hayat-i-wa ba' d-al-memat."

Zanenedwa mu Hadith sharifs kuti ndi kothandiza kwambiri kubwerezabwereza pemphero la Istighfar podziteteza ku zovuta ndi zoopsa za mtundu uliwonse ndi kuthawa zoipa ndi ziwembu za asatana ndi adani.

Moyo wanga unabwera ndi kupita ngati mphepo yokudutsa.
Kwa ine si kanthu kuma kuphethira kwa diso.
Haqq imachitira umboni: Thupi ndi malo okhala mzimu.
Tsiku lina udzauluka kuchoka mkhola yake, nga mbalame.

KALATA YA 123

Kalata iyi ya Hadrat Imam Rabbani 'quddisa sirruh' yolembedwa chifukwa cha Tahir-i-Badahshi. Ikunena kuti ntchito zopembeza za nafila, kaya ndi Haji, singakhale ya phindu ngati ikuchititsa kuti ntchito ya Fardh iphonyake:

M'bale wanga wanzeru. Kalata yamtengo wapatali yotumizidwa ndi Molla Tahir, yemwe ali woyera mofanana ndi dzina lake, yafika kuno. Mchimwene wanga! Kwanenedwanso mu Hadith Sharif kuti: "**Allahu ta'âlâ amanyansidwa ndi zofuna za kapolo Wake wotaya nthawi pa zinthu zopanda pake."** Kuchita ntchito zopembeza za nafila

mmalo mochita zomwe zili farz ndiko kugwirira ntchitonthawi pachabe. Choncho, tiyenela kuphunzira kagwilitsidwe nchito ka nthawi yathu. Tiyenera kudziwa zomwe tatanganidwa nazo. Kodi tikupembedza nafila kapena Farz? Zoletsedwa zingapo, za Haramu zimachitika p akuchita hajj ya nafila. Muyenera kuganiza bwino! Chizindikiro chabe ndi chokwanira kwa munthu wa nzeru. Ndikutumiza salaam zanga kwa iwe ndi kwa abwenzi ako.

[Zikumvekanso kuchokera mu kalata iyi kuti ma sunnat anayi mwa ma swalah asanu a tsiku lililonse, kusiyapo ma sunnat a swalah ya m'mawa, ayenera kuchitidwa ndi niyyat (cholinga) cha (kupanga) qada.]

KALATA YA ZANA NDI MAKUMI AWIRI NDI MBAMBU ZINAYI (KALATA YA 124)

Kalata iyi, inalembedwanso kwa Tahir-i-Bedahshi. Haji imakhala wajub ngati pali ndalama zoyendera. Kupita ku hajj opanda ndalama zogwiritsira ntchito pa ulendowo kumatanthauza kuwononga nthawi ndi ntchito zina. Kalata yodalitsikayi ikufotokoza mfundo iyi:

Kalata ya mtengo wapatali yotumizidwa ndi mchimwene wanga Khwaja Muhammad Tahir-i-Bedahshi yafika kuno. Hamd (kutamanda ndi kuthokoza) ndi kuyamika kukhale kwa Allahu ta'âlâ ta'âlâ (chifukwa cha madalitso Ake) kuti palibe ulesi m'chikondi (Chanu) pa faqir ndi kugwirizana nawo. Kuchedwa kwa masiku opatukana sikudatsegule njira ya zimenezo (kusintha kukhala koipitsitsa).

Mkhalidwe wanu uwu ndi chizindikiro cha chisangalalo chachikulu. Eee! m'bale wanga, amene umatikonda! Mwaganiza zopita kukapempha chilolezo. Pamene tinkasiyana, tinkaganiza kuti mwina tipeza madalitso okumana nanu m'njira. Koma, ma Istikhara omwe tinapanga pamenepo sanabwere ndi zizindikiro zovomereza. Kotero kunali kosasimikizika kuti ulendowu unalolezedwa. Choncho tinasintha maganizo athu. Zisanachitike izi, ulendo wanu nawonso siunali wovomerezeka. Koma, munali wosangalala kwambiri moti kukhumudwa koonekera kunabisidwa. Kuyamba (ulendo umenewo) kumadalira kukhala ndi ndalama za pa ulendo. Ngati munthu sangakwanitse kukwaniritsa izi, ndiye kuti wangowononga nthawi yake yochita zinthu zina popita ku haji yosapindula. Chimodzi mwa zofunika zikhalepo pochita Haji ndi ndalama zapaulendo. Mwa zina zoti zikwaniritsidwe, zili wajib kwa Msilamu kukhala ndi ndalama kuti

Haji ikhale farz kwa iye.) Kupita ku Haji sikudzakhala farz kwa munthu pokhapokha ngati ali ndi ndalama zochitira pa ulendo wa Haji. Ngati akapitabe ku Haji (popanda ndalamazo), ndiye kuti wachita Haji ya nafila (yongoonjezera). Kunena zoona, si ntchito ya farz kapena wajib kupita pa Umra. Ndiye kuti ndi mchitidwe wopembedza wa nafila. Ndipo kuchita ntchito zopembedza za nafila, posiya farz kapena kumchititsa wokhulupirirayo kuchita haram, sikukhalanso kupembedza kofunikira. Kumakhala kopanda phindu ndikukhala uchimo. [Chonde onani kalata ya makumi awiri mphambu zisanu ndi zinayi (29), yomwe siyinatanthauzidwepo m'Chichewa mpaka lero!] Sichingakhale choyenera kuchita chinthu chomwe sichili farz po kunyalanyaza mchitidwe umene uli farz. Ndinatchula mfundo zimenezi m'makalata anga ochepa. Sizikudziwika ngati mwanawalandira. Tilekere pomwepa. Inu mukudziwa chochita ndi ena onse. Wa-s-salam. [pali nkhani zokhudza Hajji mu kalata ya 250, yomwe siyinatanthauzidwe m'Chichewa mpaka pano]